Buku la Mbusa wa Chipentecoste

KALOZERA WA ABUSA A KU AFRIKA

BUKU LA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

KALOZERA WA ABUSA A KU AFIRIKA

Denzil R. Miller, Mkonzi
Jeffery Nelson, Wothandizira Mkonzi
Todd Churchill, Wothandizira Mkonzi

Buku la Mbusa wa Chipentekoste: Kalozera wa Abusa a ku Afirika
©Maumwini 2022 ndi Africa's Hope, Springfield, Missouri, USA. Maumwini onse ndi otetezedwa. Palibe gawo la m'buku ili lomwe lingatulutsidwe, kusungidwa mmalo obwezeretsa dongosolo, kapena kufalitsa mu njira iliyonse (yamagetsi, yamakina, kope, kujambula, kapena mwinamwake) popanda chilolezo cholembedwa ndi eni ake a maumwini, kupatulako mau achidule ogwiritsidwa ntchito mogwirizana ndikupereka ndemanga kapena zowunikira mu magazini, nyuzipepala, kapena zapa webusaiti.

Malembo onse atengedwa, pokhapokha atawonetsedwa, akuchokera
Buku Lopatulika ndilo Mau a Mulungu. Maumwini ©1922, 1966, 2014, 2018 ndi Bible Society of Malawi. Kugwiritsidwa ndichilolezo cha Bible Society of Malawi.

Komiti ya Akonzi:
Denzil R. Miller, DMin, Mkonzi
Jeffery Nelson, PhD, Wothandizira Mkonzi
Todd Churchill, Wothandizira Mkonzi

Kalozera wosungira mkhokwe yamabuku:
Miller, Denzil R., Mkonzi, 1946
Buku La Mbusa wa Chipentekoste: Kalozera wa Abusa a ku Afirika/ Denzil R. Miller ndi Jeffery Nelson ndi Todd Churchill

1. Practical Theology. 2. Pastoral Theology. 3. Handbooks. 4. Manuals

Translation Team:
Michael Pamfwiri Mkandawire, PhD, Mkonzi
Joseph Chimowa Phiri, DMin
Billy Malija Banda
Moses Zimba
Elijah King Nsato
Leviticus Philip Chilare
Peter Kukada
Innocent Joram

Lofalitsidwa ndi Africa's Hope
580 West Central Street
Springfield, Missouri, USA 65802

Lotsindikizidwa ku United States of America

Zam'katimu

Mndandanda wa Othandizira 7
Mau Oyambirira ndi Randel Tarr 11
Mau Oyambirira ndi Dr. Barnabas Mtokambali 13
Mau Oyamba 15

Gawo 1 ~ Zoyenereza za Mbusa wa Chipentekoste
Mutu 1 ~ Munthu Okumana Ndizochitika 23
Mutu 2 ~ Munthu wa Mzimu 33
Mutu 3 ~ Munthu Wakhalidwe Labwino 43
Mutu 4 ~ Munthu Amene Wakonzekera Bwino 53

Gawo 2 ~ Zinthu Zofunikira Zoyambirira za Mbusa wa Chipentekoste
Mutu 5 ~ Zofunikira Zoyambirira Za Utumiki 65
Mutu 6 ~ Zofunikira Zoyambirira Pa Moyo 75
Mutu 7 ~ Zofunikira Zoyambirira pa Banja 85
Mutu 8 ~ Kufunikira Kwa Pemphero 95

Gawo 3 ~ Zikhulupiriro za Mbusa wa Chipentekoste
Mutu 9 ~ Amakhulupirira Baibulo 107
Mutu 10 ~ Amalimbikitsa Choonadi cha Chipentekoste 117
Mutu 11 ~ Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekoste 127
Mutu 12 ~ Amayamikira Cholowa cha Chipentekoste 137

Gawo 4 ~ Moyo wa Mbusa wa Chipentekoste
Mutu 13 ~ Moyo Wosamalidwa Bwino 149
Mutu 14 ~ Maubale Abwino 159
Mutu 15 ~ Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu 169

Gawo 5 ~ Utumiki Owonekera wa Mbusa wa Chipentekoste
Mutu 16 ~ Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu 181
Mutu 17 ~ Kuphunzitsa Kwabwino 191
Mutu 18 ~ Kutsogolera Mpingo M'kulambira 201
Mutu 19 ~ Kutsogolera Mpingo ku Chitsitsimutso cha Chipentekoste ... 211
Mutu 20 ~ Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu 221
Mutu 21 ~ Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu 231
Mutu 22 ~ Kumenya Nkhondo za Uzimu 241

Gawo 6 ~ Mbusa Wa Chipentekoste ngati Oweta Nkhosa
Mutu 23 ~ Kumvetsetsa Utumiki wa Mbusa 253
Mutu 24 ~ Kusamalira Nkhosa 263
Mutu 25 ~ Kulimbikitsa Thupi la Khristu 271
Mutu 26 ~ Kupereka Uphungu Kwa Anthu a Mulungu 281
Mutu 27 ~ Kuteteza Nkhosa 293

Gawo 7 ~ Mbusa wa Chipentekoste ngati Mtsogoleri
Mutu 28 ~ Utsogoleri wa Chipentekoste 305
Mutu 29 ~ Utsogoleri Wotumikira 315
Mutu 30 ~ Utsogoleri Wamasomphenya 325
Mutu 31 ~ Utsogoleri wa Utumwi 335

Gawo 8 ~ Mbusa wa Chipentekoste monga Owongolera
Mutu 32 ~ Kusamalira Zolemba, Zachuma, ndi Katundu 347
Mutu 33 ~ Kusonkhanitsa Atsogoleri Omwe si Abusa 357
Mutu 34 ~ Kutsogolera Nthambi za Mpingo 367
Mutu 35 ~ Kuyang'anira Umembala wa Mpingo 379

Gawo 9 ~ Mbusa wa Chipentekoste pa Utumwi

Mutu 36 ~ Kumvetsetsa Kachitidwe ka Zinthu M'chipangano Chatsopano 391

Mutu 37 ~ Kulalikira Otayika 401

Mutu 38 ~ Kutumikira Dera Lanu 413

Mutu 39 ~ Kudzala Mipingo Yatsopano 423

Mutu 40 ~ Kukhazikitsa Dongosolo La Utumwi La Mpingo Wapamalo .433

Gawo 10 ~ Mbusa wa Chipentekoste ndi Miyambo ndi Masakaramenti

Mutu 41 ~ Kuyendetsa Mwambo wa Ukwati ndi Maliro 445

Mutu 42 ~ Kuchititsa Masakramenti, Kudalitsa Ana ndi Kukhazikitsa Atsogeleri 455

Zowonjezera

Zowonjezera 1 ~ Chiganizo cha Chikhulupiriro cha Chiyanjano cha Assemblies of God pa Dziko Lonse 467

Zowonjezera 2 ~ Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10 471

Zowonjezera 3 ~ Chidule cha Mabuku a M'baibulo 473

Mndandanda wa Othandizira

Munsimu muli mndandanda wa anthu omwe analemba nawo buku ili. Manambala omwe akuwoneka kutsogolo kwa dzina la munthu akufotokozera mutu kapena mitu yomwe munthuyo anathandizirapo kwakukulu.

Adade, Ayi, PhD. Mlembi Wamkulu, Togo Assemblies of God (29)

Ama, UcheChukwu. Wachiwiri kwa Wapampando, Africa Assemblies of God Alliance World Missions Commission (40)

Banda, Lipenga. Mtsogoleri Wamkulu, Assemblies of God in Zambia (33)

Bogere, Richard, PhD. Woyambitsa Nawo, Christ Chapel International, Kampala, Uganda; Mphunzitsi, Pan Africa Theological Seminary (6)

Bomboko, Cécile, PhD. Nthumwi ya Chigawo Chapakati mu Afirika, Association for Pentecostal Theological Education in Africa (APTEA) (14, 32)

Bomboko, Marcel, PhD. Wapampando, Bungwe la Abwanamkubwa, West Africa Advanced School of Theology, Lomé, Togo (14, 32)

Chipao, Lawrence, PhD. Mphunzitsi Wamkulu wa zauzimu, Malawi Assemblies of God University (34)

Churchill, Todd. Mtumwi wa AGWM ku DR Congo, Africa's Hope (30)

Daplex Ouentchist, Honoré, PhD. Pulezidenti, Evangelical Church of the Assemblies of God, Cotê d'Ivoire (10)

Djakouti, Mitré. Pulezidenti, Togo Assemblies of God; Pulezidenti Wakale, Africa Assemblies of God Alliance (15)

Dube, Andrew, PhD. Pulezidenti, Malawi Assemblies of God (11)

Flindja, Douti Lallebili, PhD. Mkulu wa Maphunziro, West Africa Advanced School of Theology, Lomé, Togo (27)

Frimpong-Manso, Paul, PhD. Mtsogoleri Wamkulu, Assemblies of God, Ghana (37)

Gnanchou, Désiré Béchié, PhD. Pulezidenti Wakale, Evangelical Assemblies of God, Cotê d'Ivoire; Wotsogolera, Theological and Pastoral Institute of Katadji (23)

Kitoto, Dinah. Wife of Philip Kitoto, Mtsogoleri Wamkulu, Kenya Assemblies of God (7)

Kitoto, Philip. Mtsogoleri Wamkulu, Kenya Assemblies of God; Mtsogoleri, KAG East University (7)

Kuoh, Jimmy, PhD. Mtsogoleri Wamkulu Opuma, Assemblies of God Liberia; President, Liberia Assemblies of God Bible College (21, 41)

Lebelo, Gordon, PhD. Mtsogoleri Wamkulu, International Assemblies of God, South Africa (26)

Lwesya, Enson, DMin. Mtsogoleri Wamkulu, Malawi Assemblies of God University (28)

Mba, Arthur, PhD. Wachiwiri kwa Wapampando oyamba, Assemblies of God, Gabon (2, 18)

Mbiwan, Daniel. Mtsogoleri Wamkulu, Full Gospel Mission, Cameroon (25)

Miller, Denzil R., DMin. Mtumwi wa AGWM; Wotsogolera, Acts in Africa Initiative (1, 3, 8, 16, 20, 36)

N'sembe Loyela, Israël. Mbusa, Ark of the Covenant Evangelistic Center, Kinshasa; Mtsogoleri Wamkulu Wakale, Assemblies of God, DR Congo (22)

Ndayisaba, Jérôme. Pulezidenti, Burundi Assemblies of GodFellowship (24)

Nelson, Jeffery, PhD. Mtumwi wa AGWM; Mtsogoleri Wamkulu Wakale, KAG East University, Nairobi, Kenya (5, 12, 39)

Ngabonziza, Emmanuel. Wachiwiri kwa Mtsogoleri Wamkulu, Pentecostal Assemblies of God, Rwanda (38)

Niba, Felix, PhD. Wotsogolera Utumwi wa Kunja, Full Gospel Mission, Cameroon (13)

Oganya, Ngozi Cecilia, PhD. Woyendetsa Theological Education by Extension (TEE), Assemblies of God Divinity School, Umuahia, Nigeria (17)

Sawadogo, Jephté, DMin. Wachiwiri kwa Wapampando, Burkina Faso Assemblies of God; Wotsogolera, Koubri Bible School (4, 42)

Sebastião, Francisco. Pulezidenti, Angola Assemblies of God (9)

Smith, Bernard, MA. Mtumwi wa AGWM ku Togo (15)

Swai, Ron. Msungi Chuma Wamkulu, Tanzania Assemblies of God (35)

Turney, Mark, MA. Mtumwi wa AGWM; Pulezidenti, West Africa Advanced School of Theology, Lomé, Togo (19)

Watt, C. Peter, ThD. Wapampando, Assemblies of God, South Africa (31)

Mau Oyambirira ndi Randel Tarr

Buku la Mbusa wa Chipentekoste limalonjeza kutumikira ngati katundu ofunikira kwambiri kwa Mbusa wa ku Afirika kwa zaka zamtsogolo. Mpingo wa mu Afirika wakhala ukufunikira zinthu zotere, zimene zimakamba za zovuta zomwe zimakhudza Abusa a Chipentekoste ku Afirika.

Mu ntchito yake, Dr. Denzil R. Miller ndi gulu lake lolemba, Dr. Jeffery Nelson ndi Todd Churchill, anasonkhanitsa mndandanda wagulu la atsogoleri ochititsa chidwi aku Afirika kuti alankhulepo pa nkhani zambiri zimene abusa a CHIPENTEKOSTE amakumana nazo lero lino ku Afirika. Monga "mndandanda wa anthu othandizira" ukuonetsera poyambirira pa bukuli, mndandanda uwu ukuphatikizapo atsogoleri a mpingo mu dziko, abusa otsogolera, oyendetsa komanso aphunzitsi a Sukulu za Baibulo ndi ma seminare, atsogoleri a utumwi, odzala mipingo, alaliki ndi ena ambiri.

Kuzama kwa kudziwa ndi chidziwitso cha atsogoleriwa kukuonjezera kufunikira kwakukulu kwa ntchito iyi. Pogwirapo limodzi ntchito ndi ambiri mwa anthu awa, ndikhoza kutsimikizira za ungwiro wawo ngati atsogoleri, mtima wawo pa Khristu ndi utumiki wake, ndi kukhumba kwawo kofuna kuti awone mpingo ukudzalidwa mu dera lililonse la mu Afirika. Kuonjezera apo, gulu limene linaunikanso zolembedwa palokha likubweretsa chidziwitso chamtengo wapatali cha Afirika ndi anthu ake pa kukonza kwa bukuli. Aliyense wa iwo akhala akutumikira ngati mtumwi kummwera, kummawa kapena pakati pa Afirika.

Buku ili limalonjeza kulimbikitsa mautumiki a iwo amene akutsogolera kale mipingo ya pamalo mu Afirika, komanso iwo amene ali mu sukulu za Baibulo ndi omwe akuchita maphunziro awo a Baibulo mmadera pokonzekera utumiki wa mtsogolo. Bukuli ndilodzazidwa ndi zothandiza zogwirika zomwe zidzathandizire Mbusa wa Chipentekoste kuti achite bwino mu utumiki ndi kubala zipatso zochuluka zomwe zidzakhale zokhalitsa.

Chotsindika chimodzi chapaderadera cha bukuli ndi mayitanidwe ake kwa Mbusa wa Chipentekoste ku Afirika kuti akhale mzibambo kapena mzimayi wa chikhalidwe chapamwamba. Chotsindika china chofunikira ndi kupempha nthawi zonse kokhazikika kwa bukuli kwa Mbusa wa ku Afirika kuti akhale odzazidwa

ndi Mzimu Woyera komanso kuti akhale wachindunji pa cholinga choperekedwa ku mpingo ndi Mulungu powona kuti mwamuna aliyense, mkazi ndi mwana mu Afirika, apatsidwe mwayi wakumva Uthenga Wabwino ndi kukhala ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu. Ndizolimbikitsa kuona maonedwe achindunji pa utumiki mu bukuli m'nthawi ino yomwe "uthenga wakulemera" watsogolera mipingo yochuluka mu Afirika kuchoka pa cholinga cha Mulungu posakasaka madalitso a munthu payekha. Othandizira pa bukuli ndi anthu amene akuchita moonadi Mau, abambo ndi amayi a Mulungu amene akufuna kukhala pachindunji cha Kutuma Kwakukulu kwa Khristu mu moyo wawo wa tsiku ndi tsiku.

Mu zaka 60 zapitazo ndakhala ndikulumikizana ndi mpingo waku Afirika, poyamba ngati mwana okulira mu Afirika ndipo kenako ngati mtumwi ku Mvuma kwa Afirika kwa zaka zoposera 35. Ndizosangalatsa kuona zimene Mulungu wachita kudzera mu ntchito ya zikwi za abambo ndi amayi a mu Afirika amene apatula miyoyo yawo kuti apindule miyoyo yotayika posatengera mtengo wake. Ndikukhulupirira kuti buku ili ligwira ntchito yopititsa patsogolo kuchita bwino kwawo mu utumiki. Pemphero langa ndi lakuti, pamene buku ili likuyikidwa mmanja mwa zikwi za abusa ndi ophunzira a sukulu za Baibulo mu Afirika yense, ufumu wa Mulungu ufika ku dzikolo mochulukira.

Chiyembekezo chenicheni cha Afirika ndi atsogoleri opatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera komanso ophunzitsidwa bwino Baibulo!

~ Rev. Randel Tarr
Wotsogolera Wamkulu
Africa's Hope

Mau Oyambirira ndi Dr. Barnabas Mtokambali

Abusa ambiri a ku Afirika akhoza kuzizindikiritsa okha ndi kaganizidwe ka Paulo pamene ankalembera kwa Akhristu aku Akorinto:

“Paulendo kawirikawiri, moopsa mwake mwa mitsinje, moopsa mwake mwa … m'chivutitso ndi m'cholemetsa, m'madikiro kawirikawiri, m'njala ndi ludzu, m'masalo a chakudya kawirikawiri, m'chisanu ndi umaliseche. Popanda zakunjazo pali chondisindikiza tsiku ndi tsiku, chalabadiro cha Mipingo yonse” (2 Ako. 11:26-28).

Ngakhale nyengo zawo zikhoza kusiyana ndi za Paulo, abusa ambiri a mu Afirika akhoza kudzifanizira ndi mamvedwe ake “osautsika monsemo” (4:8).

Pali ntchito zochepa zomwe ndizovutirapo kuposera ubusa mu mpingo wa Chipentekoste ku Afirika. Taganizirani za magawo ambiri a moyo momwe Mbusa wa Chipentekoste akuyenera kuonetsera kuthekera kuchita bwino. Iye ayenera kukhala othekera kukwaniritsa kusamalira nkhosa za Mulungu, pamenenso akukwaniritsa kuyendetsa bwino banja ndi moyo wawo. Akuyenera kukhala okwanitsa kulalikira, kuphunzitsa, kupereka uphungu ndi kuyendetsa zinthu bwino—zonsezi pa nthawi imodzi. Muzonsezi, akuyenera kumatsogolera mipingo yawo pokwaniritsa lamulo la Ambuye Yesu Khristu lopanga ophunzira a mitundu yonse. Mndandanda ukhoza kumapitirira. Ndi chifukwa chake kubwera kwa buku ili la Mbusa wa CHIPENTEKOSTE lili lolandiridwa.

Kwa nthawi yayitali ndakhala ndikuona kufunikira kolembedwa buku la Mbusa kuchokera ku maonedwe ndi kaganizidwe kaku Afirika ndi Chipentekoste. Kotero ndine oyamika kwambiri chifukwa cha ntchito imene yachitidwa ndi Africa’s Hope popanga buku ili. Cholimbikitsa kwambiri ndi chakuti buku ili lalembedwa ndi abusa akuluakulu a Chipentekoste ndi atsogoleri a m’maiko onse a mu Afirika. Panthawi yomweyo zolembedwa mu buku ili ndi zomveka bwino pa maphunziro a za umulungu, zachindunji pa utumwi komanso zothandiza. Bukuli likupereka kwa Mbusa wa Chipentekoste chidziwitso chochuluka cha moyo wa Mbusa wa Chipentekoste ndi utumiki. Lithandizira kutsogolera Mbusa wa Chipentekoste mu Afirika kuti akhale ochita bwino mu utumiki. Ndipo pambali

polimbikitsa manja aabusa athu, zidzalimbikitsa mipingo imene iwo akuyitsogolera.

Ndikuyembekezera kuti *Buku la Mbusa wa Chipentekoste* likhala lothandiza makamaka mnthawi iyi ya Africa Assemblies of God Alliance (AAGA) "zaka za Chitsitsimutso" zotsindikidwa kuchokera mu chaka cha 2021 mpaka 2030. Mu zaka khumi zimenezi, mipingo ya Assemblies of God mu Afirika yense ikudzipereka yokha kufunafuna Mulungu kuti apereke Mzimu Woyera mwa mphamvu ku mpingo, zomwe zingatsatiridwe ndi chitsitsimutso chachikulu chomwe sichinaonekenso mu Afirika, kupereka mphamvu kwa okhulupirira kuti atengere uthenga wabwino kwa mtundu ulionse, fuko, ndi anthu, kubwera kwa Khristu kusanachitike posachedwapa.

Muzaka za chitsitsimutsochi, mipingo ya Assemblies of God idzakhala ikulunjika pa patsidwa mphamvu ya Mzimu Woyera, kukhala moyo wa umulungu, kuphunzitsa, kufalitsa uthenga, kudzala mipingo, ndi kuchita utumwi kwa anthu amakhalidwe osiyanasiyana pakati pa osafikiridwa ku Afirika—makamaka ku Mpoto kwa Afirika. Ndili ndi chikhulupiriro kuti *Buku la Mbusa wa Chipentekoste* lidzatumikira kukhala chida chofunikira kwambiri, kuthandizira abusa kukwaniritsa cholinga chachikulu. Ngati Ambuye angachedwe pa kubweranso kwake, bukuli lidzakhala likupitirira kutumikira mipingo ya Chipentekoste mu Afirika kwa zaka zambiri zikubwerazo.

Ndine okondwa polimbikitsa za bukuli kwa abusa a Chipentekoste ndi atumiki mu Afirika yense.

~ Dr. Barnabas Mtokambali
Wapampando
Africa Assemblies of God Alliance

Mau Oyamba

Powona momwe mpingo waku Afirika ukukulira, mtsogoleri wina analankhula, “Mulungu akudalitsa mpingo waku Afirika ndi cholinga chakuti mpingo wa ku Afirika ukhoza kudalitsa mafuko ena!” Ife a ku *Africa’s Hope Acts 1:8 Initiative* timagwirizana kwathunthu ndi mfundo imeneyi. Tikukhulupirira kuti Mulungu waitana mpingo wa ku Afirika mu Ufumu pa nthawi ngati imeneyi (fanizilani Estere 4:14). Mpingo wa Chipentekoste mu Afirika uli nditsogolo lalikulu la utumwi. Mu masiku ano a nthawi yotsiriza, Mbuye wa kholola akutsanulira Mzimu Woyera pa anthu ake kuwapatsa mphamvu kuti akhale nacho chiyembekezo chokwaniritsa Kutuma kwake Kwakukulu Iye asanabwere kuchokera kumwamba (Mateyu 24:14; Machitidwe 1:8-11).

Kuti izi zichitike, mpingo wa ku Afirika ukuyenera kuti ukhale olimba. Ndipo pokhala olimba, uyenera kukhala ndi utsogoleri olimba. *Buku la Mbusa wa Chipentekoste* linapangidwa ndi cholinga chofuna kukwaniritsa chosowa ichi. Linapangidwa kuti likonzekeretse Mbusa wa Chipentekoste wa mu Afirika ndi cholinga chakuti achite mbali yawo pokwaniritsa cholinga cha Mulungu pa mpingo. Chiyembekezo chathu ndi chakuti buku ili likhala lofunikira kwambiri m'manja aabusa a Chipentekoste mu Afirika yense. Bukuli lapangidwa ndi malingaliro a mfundo 6 kuti zitsogolere:

1. Liri ndi Kaonedwe ka m’baibulo. Olemba buku ili akukhulupirira kuti Baibulo ndi Mau a Mulugu ovumbulutsidwira kwa anthu. Ndi chotsogolera chokwanira cha moyo wa Chikhristu ndi utumiki. *Kotero,olemba buku ili kufunitsitsa kwao nkuti* akhazikitse molimba maganizo alionse mu buku ili pa Malembo.

2. Ndi la Chipentekoste mu kutsindika kwake. Bukuli linalembedwa ndi abusa a Chipentekoste chifukwa cha abusa a Chipentekoste. Likufunitsitsa kuti likambe zokhudza za paderadera za abusa a Chipentekoste mosazembayitsa kuchokera pa kaonedwe ka Chipentekoste. Aliyense mwa othandizira polemba buku ili ndi mtsogoleri okhwima wa Chipentekoste omwe ali ndi utumiki ozindikirika. Chifukwa cha chidziwitso chawo ndi Mzimu, ndi kumvetsetsa kwawo pa malembo, abambo ndi amayiwa ali ndi kafikiridwe ka Chipentekoste pa moyo ndi utumiki. Izi zikuonetseredwa mu ntchito yonseyi.

3. Ndi la utumwi mu chindunji chake. Olemba bukuli akukhulupirira kuti Mulungu akulamulira Mbusa wina aliyense wa Chipentekoste kuti atenge nawo mbali pa cholinga cha Mulungu. Cholinga cha Mulungu ndi kuombola ndi kudziyitanira kwa iye yekha anthu a mitundu yonse, chilankhulo ndi fuko pa dziko lapansi Yesu asanabwerenso (Mat. 24:14; Chiv. 5:9). Khrsitu anaomba nkota pa cholinga cha Mulungu pa mau ake a Kutuma Kwakukulu (Mat. 28:18-20; Marko 16:15-17; Luka 24:47-49; Yohane 20:21-22; Machitidwe 1:8). Kutsindika kwa utumwi kukulimbikitsidwa mu buku lonseli.

4. Ndi logwirizana ndi kalankhulidwe ka mu Afirika. Gulu loyembekezereka kufikiridwa ndi *Buku la Mbusa wa Chipentekoste* ndi abusa a Chipentekoste mu Afirika. Olemba akumvetsetsa kuti Mbusa waku Afirika amachita utumiki wake molingana ndi ku Afirika. Ndipo amachita izi molingana ndi zovuta zapaderadera za ku Afirika ndi zowakhudza. Gawo lililonse lalembedwa ndi malingaliro oterewa.

5.Ndi otambasulidwa bwino maonekedwe. Buku ili lakonzedwa ndi cholinga chakuti likhudze nkhani zochulukirapo zomwe amakumana nazo abusa a Chipentekoste aku Afirika lero. Chiyembekezo cha olemba ndi chakuti likhala lofunikira kwambiri mmanja mwa abusa a ku Afirika mu Afirika yense.

6. Ndi logwirika mu kagwiritsidwe ntchito. Pamene buku ili likufotokoza nkhani za maphunziro a umulungu aabusa ndi maganizo, maphunziro ofotokozeredwa umu apangidwa kuti akhale ogwirika powachita. Sakungokamba *zimene* Mbusa wa Chipentekoste akungoyenera kuchita kokha ayi, komanso *chifukwa* chimene akuyenera kuzichitira, ndi *momwe* akhoza kupitirizira kuzichita bwino mu mautumiki awo.

Ndondomeko ya Kalembedwe

Buku la Mbusa wa Chipentekoste linayambitsidwa ndi Dr. John Easter, nthawi imeneyo anali Wotsogolera Wamkulu wa utumiki wa Africa's Hope ndipo anakhazikitsa komiti yoti ipange buku ili. Randy Tarr, yemwe ndi mlowammalo wa Dr. Easter, anapitiriza ntchitoyi.

Ntchito yoyambirira ya komiti inali kuyika mndandanda wa mitu imene bukuli likhale likukamba. Iyi inali ntchito ya nthawi yayitali pokambirana moona mtima ndi kuchita kafukufuku. Mndandandawu unaperekedwanso kwa atsogoleri ofunikira mu Afirika ndi a zamaphunziro mu Afirika yense. Pamapeto pake mitu

42 ya mu buku ili inasankhidwa. Pamene mutu unatsimikidwa komiti inayika izi mu magulu okwana khumi, amene anakhala magawo 10 a bukuli.

Atasankha mitu yomwe ikambidwe, komanso mmene iwonekere mu bukuli, komiti inasankha abusa ofunikira a Assemblies of God, a zamaphunziro, ndi atsogoleri a mipingo ochokera mu Afirika yense kuti alembe mitu paokhapaokha. Atumwi amene akhala akutumikira ku Afirika anayitanidwanso kuti alembe nawo. Maina a anthu olembewa, komanso ndi mbiri yawo, zikuoneka pa "mndandanda wa othandizira" pafupi ndi koyambirira kwa bukuli.

Mlembi akamaliza ntchito yake, amapereka ntchitoyo kwa a komiti kuti ayiunike ndi kuikonza. Komiti kenako imaunika mutu ulionse kuona nkhani komanso kulumikizana kwa mutu ndi mitu ina. Cholinga chawo chinali chakuti aonetsetse kuti zolembedwa mu mutu zinali kuonjezera pa cholinga cha Chipentekoste mu bukuli, komanso kuonetsetsa kuti kalembedwe kanali kogwirizana ndi ntchito yonse. Pamene ntchito yokonzanso inatha, mutu umaphatikizidwa kukhala gawo la buku.

Kagwiritsidwe Ntchito ka Mulowa Mmalo

Mau akuyenera kuti alankhulidwepo okhudzana ndi kagwiritsidwe ntchito ka mau "iye" mu buku ili pamene tikukamba za Mbusa wa Chipentekoste mu Afirika. Mchitidwewu unalondoledwa pofuna kuonetsetsa kuti kukula kwa chiwerengero cha abusa a chizimayi omwe akutumikira mu mipingo ya Chipentekoste mu Afirika, utumiki wao ukunyadiridwa komanso kuyamikiridwa.

Kuchokera pa kukhazikitsidwa kwake, gulu la Chipentekoste lakhala likulemekeza kufunikira ndi malo a utumiki wa amayi. Achipentekoste amakhulupirira kuti Mzimu yemwe amapereka zoyenerereza kwa abambo ku utumiki ndi Mzimu yemweyonso amene amayenerezanso amayi. Amakhazikitsa chikhulupiriro ichi pa lonjezo la Machitidwe 1:8, Pamene Iye akulonjeza Mzimu Woyera kwa okhulupirira onse, abambo ndi amayi. Aliyense amene analandira Mzimu Woyera, kuphatikizapo amayi, analandira mphamvu yokhala mboni ya Khristu. Umboni uwu ukhudzana ndi kulalikira kwa uthenga wabwino.

Achipentekoste amatchulanso lonjezo la mneneri Yowele lotchulidwa ndi Petro pa Tsiku la Pentekoste: "ndipo kudzali mu m'masiku otsiriza, anena Mulungu, ndidzathira cha Mzimu wanga *pa thupi lililonse*, ndipo ana anu aamuna, ndi a*akazi* adzanenera, … ndiponso pa akapolo anga ndi pa *adzakazi* anga m'masiku awa ndidzathira cha Mzimu wanga; ndipo adzanenera (Mach. 2:17-18,

kutsindika kwaonjezedwa; fanizilani Yowele 2:28-29). Achipentekoste amatenga chiganizo ichi kukhala mfundo ya dziko lonse kwa okhulupirira ndipo amachitapo kanthu mu nthawi iyi "Nyengo ya Mzimu" pamene Mulungu akupereka Mzimu wake mwa chisomo kwa anthu onse.

Kuchokera mu mbiri, alembi a chingerezi amagwiritsa ntchito mlowammalo "iye" kapena "iwo" pokamba zoimirira onse amuna kapena akazi. Popewa chisokonezo, mkonzi wasankha kugwiritsa ntchito mau ophatikiza akuti "iye" pokamba za abusa a Chipentekoste. Pazifukwa zoti ziwerengedwe bwino, izi zimafunikira kuti mlowamalo wa ambiri "iwo" nthawi zina agwiritsidwe ntchito mmalo mwa munthu mmodzi "iye." Izi ndizovomerezedwa kwambiri pakati pa alembi a chingerezi masiku ano, ndipo ndi mchitidwe wa kamasulidwe ka baibulo la tsopano.

Kagwiritsidwe Ntchito ka Bukuli

Monga dzina lake likufotokoza, bukuli lakonzedwera abusa a CHIPENTEKOSTE a ku Afirika. Mukhoza kugwiritsa ntchito bukuli mu njira zothandiza zosiyanasiyana. Poyamba, mufunika muliwerenge bukuli kuchokera pa chiyambi mpaka ku mapeto. Izi zikupatsani chithunzithunzi chachikulu cha maganizo okambidwa mu bukuli. Zikuthandiziraninso kuti mupeze chidziwitso chachikulu ku mbali zambiri za ntchito ya Mbusa wa CHIPENTEKOSTE mu Afirika.

Pamene mukhale mkuyenda mu bukuli, muyenera kukhala ndi polemba ndi cholembera ndi cholinga chakuti mudzitha kulemba mfundo zimene zakukhudzani pa moyo wanu komanso mu utumiki. Mudzafunikanso kuti mudzilemba maganizo anu pa mutu omwe ukukambidwa panthawiyo. Mudzazindikira pa zomwe mukuyenera kusitha pa kachitidwe ka momwe mumachitira utumiki. Pomaliza, komanso chofunikira kwambiri, pamene mukuwerenga, mukuyenera kumamvetsera ku liu la Mzimu, komanso kuona zimene akukulankhulani. Kenako mudzafunika kuti mudzagwiritse ntchito buku lanu lolembamo ngati chokutsogolerani popemphera komanso chothandizira chotsogolera pokonzanso utumiki ndi moyo wanu.

Mukhoza kugwiritsa ntchito buku ili ngati lokuthandizira pa zina. Pamene pali chochitika chapaderadera ngati ukwati, maliro, gawo lopereka uphungu, msokhano wa atsogoleri kapena zochitika zilizonse, mukhoza kupita pa mutu okhudzidwa ndi kuunikanso kuti mupeze chitsogozo cha chidziwitso chake.

Pamene mukusowekera thandizo kuti mukonze vuto limene lilipo kapena kuyamba ntchito ya utumiki yatsopano, mukhoza kufufuza pa tsamba la za Zamkatimu kuti mupeze mutu umene ukukamba za nkhaniyo.

Pomaliza, bukuli litha kugwiritsidwa ntchito ndi aphunzitsi aku sukulu za Baibulo ngati buku lophunzirirapo kapenanso loonjezera pa maphunziro awo a ubusa. Bukuli litha kukhala lothandiza kwambiri maka mu sukulu za nthawi yochepa monga ngati maphunziro a Baibulo ochitika ndi Nthambi ya sukulu ya Baibulo kapena sukulu zodzala mipingo.

Ife, a komiti yoyendetsa *Buku la Mbusa wa Chipentekoste* tikulimbikitsa za ntchito iyi kwa abusa a Chipentekoste ku Afirika. Ndipemphero lathu kuti Mulungu aligwiritsa ntchito kuti lidalitse abusa aku Afirika kwa zaka zikubwerazo, ndikuti buku ili lidzagwiritsidwa ntchito ngati chida chofunikira popititsa ufumu wa Mulungu patsogolo ku Afirika, ndi mipingo yonse yaku Afirika, ku mafuko.

Mwaulemu,
~ Dr. Denzil R. Miller, mkonzi
~ Dr. Jeffery Nelson, mkonzi wothandizira
~ Rev.Todd Churchill, mkonzi wothandizira

~ Gawo 1 ~

ZOYENEREZA ZA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

~ Mutu 1 ~

Munthu Okumana Ndizochitika

Taganizani za munthu amene adaphunzira za chipatala pa sukulu ya ukachenjede yapamwamba. Adakhala nawo pa maphunziro ong'amba munthu ndi kuwerenga mabuku abwino okhudza nkhaniyi. Komabe, sadang'ambepo munthu wina aliyense. Kodi mungafune kuti munthuyu achite opareshoni pa inu. Zoonadi, ayitu. Ngati wina afunitsitsa kukhala dotolo wong'amba anthu, iye akusoweka kuphunzira ndi manja ake pansi pa dotolo wina wodziwa bwino ntchitoyi.

Chimodzimodzinso, wina asanayambe utumiki wa ubusa, iye akuyenera kuphunzira mochita. Kuchita kumeneku kukhale kwa uzimu ndi kochita ntchitoyo. Mu mutuwu, tifufuza kuphunzira kochita kofunika kwa wina aliyense yemwe akufuna kukhala Mbusa wa Chipentekoste.

CHOCHITIKA CHA UZIMU

Chochitika chokumana ndi Mulungu ndi poyambira pofunikira kwa mbusa aliyense wa Chipentekoste. Pamwamba pa zonse iye akhale pa ubale wozama wayekha ndi Mulungu. Pamene Yesu adasankha Khumi ndi awiriwo, adachita ichi "kuti akhale ndi Iye" (Marko 3:14). Adadziwa kuti, pamene iwo ankayenda ndi kuyankhula ndi Iye, adzakhala ngati Iye. Yesu anati, "Aliyense akaphunzira mokwanira adzakhala ngati mphunzitsi wake" (Luka 6:40). Ndi chimodzimodzinso ndi ife lero, pamene titenga nthawi ndi Khristu mMau ake ndi

mpemphero, timakhala ngati Iye (2 Akorinto 3:18). Tisanatumikire mmalo mwa Iye, tikuyenera tikhale ngati Iye, ndipo kuti tikhale ngati Iye, tiyenera kutenga nthawi ndi Iye.

Mayendedwe a Chipentekoste adayambidwa ndi kutsimikiza mtima kuti okhulupirira lero akhoza kukumana ndi chochitika chosintha chauzimu monga adachitira atumwi ndi ophunzira ena m'Chipangano Chatsopano. A Chipentekoste amaphunzitsa kuti, pomwe chiphunzitso chorama nchofunikira, koma nchosakwanira. Kuposera zonse, ngati mbusa wa Chipentekoste, ukuyenera kukhala ndi ubale wopitirira ndi Yesu Khristu. Popanda ubale umenewu, watayidwa kunja mu utumiki. Ubale umenewu umayambidwa pokumana nacho chochitika chauzimu. Kudzera m'Baibulo, awo womwe adatumikira kwa ena adayamba ulendo wao pokumana ndi Mulungu. Abrahamu adamva liu la Mulungu (Gen. 12:1-3). Mose adakumana ndi Mulungu m'chitsamba choyaka moto (Eksodo 3:14). Yesaya adawona Mulungu m'kachisi, ali pamwamba atakwezeka (Yesaya 6:1-5). Ophunzira adayenda ndi Yesu (Marko 3:13-14). Ndipo Paulo adakumana ndi Khristu wowukayo pa njira ya ku Damasiko (Machitidwe 9:1-5).

Chimodzimodzi, aliyense yemwe akufuna kukhala mbusa wa Chipentekoste akuyenera kukhala ndi zinthu zofunikira zinayi zokumana ndi Mulungu:

Kubadwa Mwatsopano

Nikodemo anali mtsogoleri wa chipembedzo. Anali Mfarisi wodzipereka ndi membala wa bungwe lolamulira la Chiyuda. Komabe padalibe chimodzi mwa izi chimene chidali chokwanira. Yesu adamuuza Nikodemo, "Uyenera kubadwanso mwatsopano" (Yohane 3:7). Yesu adamuuza iye kuti sangathe "kulowa" kapena "kuwona" ufumu wa Mulungu pokhapokha atabadwanso kuuzimu (vv.3-5).

Mbusa aliyense wa Chipentekoste akhale wobadwadi mwatsopano. Iwo akuyenera kuchitira umboni za nthawi mmoyo wao imene adakumana ndi Yesu, kulapa machimo awo, ndi kumulandira Iye ngati Mbuye wao ndi Mpulumutsi. Panthawi imeneyo, Yesu adatenga malo Ake oyenera pa mpando wamiyoyo yawo. Paulo adalemba, "Ngati aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa mwatsopano. Zakale zapita, taonani zatsala zatsopano (2 Akorinto 5:17).

Munabadwa mwatsopano? Umunthu wanu udasinthika kuchokera mkati ndikutulukira kunja? Ngati ayi, mukhoza panopa. Tembenukani kumachimo anu ndi kupemphera, kumupempha Mulungu kuti akukhululukireni inu. Ikani kudalira

kwanu konse mwa Khristu yekha ku chipulumutso, ndi kumuyitana kuti atenge malo ake enieni ngati Mbuye wamoyo wanu. Kulandira Khristu ngati Mpulumutsi, kukhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndi kupemphera pemphero ili:

> "Yesu, ndikhulupiriradi kuti Ndinu mwana wa Mulungu, Mpulumutsi wa dziko lonse. Ndikukhulupirira kuti Mudafera machimo anga ndi kuukanso. Ndikudziwa kuti ndine wochimwa, ndipo popanda chikhulupiriro mwa inu, ndine wotayika kwa muyaya. Chonde mundikhululukire ine machimo anga ndipo mukhale Mpulumutsi ndi Mbuyanga. Tsopano ndikusiya zonse kuti nditsate Inu. Ndidzatumikira Inu masiku onse amoyo wanga. Bwerani mumtima wanga ndipo mukhale Mbuye wamoyo wanga. Mudzina lanu ndapemphera. Amen."

Ubatizo wa Mzimu Woyera

Yesu asanakwere kumwamba, adalamulira ophunzira Ake, "Khalani mumzinda kufikira mwavekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba" (Luka 24:49). Adayenera kudikira muYerusalemu kufikira atabatizidwa mwa Mzimu Woyera (Machitidwe 1:4). Anthuwa adali atabadwa mwatsopano. Adali atakhala pansi pa chiphunzitso cha Yesu, ndiponso adachitira umboni za zozwiza zake. Iye adawatuma kuti akalalikira uthenga wabwino padziko lonse lapansi. Komabe, adali osakonzeka.

Ntchito imene Yesu adawapatsa iwo inali yowakulira iwo kuti ayigwire ndi mphamvu zawo zokha. Adasoweka kudzadzidwa ndi mphamvu ya Mulungu. Yesu adawalonjeza, "Mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira mpaka malezekezero ake a dziko lapansi" (Machitidwe 1:8).

Mzimu adadza poyamba pa ophunzira ndi kuwadzadza iwo pa tsiku la Pentekoste. Panthawi imeneyo, adalankhula ndi malilime ndipo adalandira mphamvu ndi kulimbika kumeneko adakusowa kuti alalikire Khristu mochitachita, ngakhale padali chizunzo cholimba. Wina aliyense amene akukhumba kutsatira Ambuye mu utumiki akuyenera kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.

Yesu adatiuza momwe tingabatizidwire mwa Mzimu Woyera. Iye adalonjeza, "Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akumpempha Iye!" (Luka 11:13). Wina aliyense atha kulandira mphamvu ya Mzimu pakungopempha mwa chikhululupiriro. Kupempha uku kuli m'magawo atatu achikhulupiriro:

1. Pemphani mwa chikhulupiriro. Yambani kupempha Mulungu za Mzimu. Poyankhula za mphatso ya Mzimu, Yesu adalonjeza, "Pemphani, ndipo adzakupatsani; funani, ndipo mudzapeza; gogodani ndipo adzakutsegulirani" (Luka 11:9). Pamene mupempha, khulupirirani kuti Mulungu akumva ndi kuyankha pemphero lanu, ndikuti Iye panthawiyi akukudzadzani ndi Mzimu Woyera. Tsegulani kwambiri mtima kwa Mulungu, ndipo imvani kubwera kwa Mzimu pa inu. Ndipo mukangomva Mzimu pa inu, inu mwakonzeka kutenga khwelero lachiwiri la chikhulupiriro

2. Landirani mwachikhulupiriro. Yesu adalonjezanso, "Aliyense wakupempha alandira" (Luka 11:10). Panthawi ina Iye anaphunzitsa, "Zinthu zilizonse mukazipemphera ndikuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo" (Marko 11:24). Khulupirirani kuti Mulungu akuyankha pemphero lanu ndi kukudzadzani inu ndi Mzimu Woyera. Pamene muchita ichi, mumve kupezeka kwa Mzimu mkati mwanu (Yohane 7:38). Ichi chikachitika, tengani khwelero lachitatu la chikhulupiriro.

3.Lankhulani mwachikhulupiriro. Baibulo limati pa tsiku la Pentekoste "anadzadzidwa onse ndi Mzimu Woyera nayambakulankhula ndi malilime ena monga Mzimu anawalankhulitsa" (Machitidwe 2:4). Mau omwe mulankhule sakhala ayinu nokha; achokera kwa Mulungu. Achokera kunsi kwa mzimu wanu (1 Akorinto 14:2). Ndipo akhala muchilankhulo chomwe simuchidziwa. Ichi ndichizindikiro cha Mulungu kwa inu, ndi mpingo, kuti Iye wakupatsani inu mphamvu kuti mulankhule mmalo mwa Iye. Ambuye alemekezeke! Mwabatizidwa ndi Mzimu Woyera.

Kuyitanidwa kwa Kumwamba

Kukhala mbusa wa Chipentekoste zikuposera pa chisankho cha ntchito; ndi mayitanidwe ochokera kwa Mulungu. Poyankhula za Yesu, Paulo adalemba, "Iye adapatsa ena akhale atumwi, ena aneneri, ena alaliki; ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi" (Aefeso 4:11). Pamodzi ndi maudindo ena autumiki anayi, abusa ndi mphatso yoperekedwa ndi Khristu ku Mpingo wake. Ambuye mwini yekha amasankha iye amene amamuloza kuti akhale mbusa. Amasankha ndipo, kenako amayitana, namukhazikitsa. Yesu adawuza ophunzira ake, "Inu simunandisankhe Ine, koma ndinakusankhani inu, ndipondinakuikani, kuti mukamuke inu ndikubala chipatso, ndi kuti chipatso chanu chikhale" (Yohane 15:16).

Ambuye adavumbulutsa zoonadi zofunikira zitatu zokhudza mayitanidwe a Mulungu: Choyamba, adavumbulutsa kuti ndi Mulungu yekha amene amasankha. Mbusa weniweni wa Chipentekoste samadzisankha yekha. Iye amasankhidwa ndi Khristu. Popitiliza Yesu adavumbulutsanso kuti ndi Iye amene amapereka ntchito za utumiki. Adapitiliza, "Ndinakusankhani Ine, ndi kuloza inu." Khristu sangosankha amene akamutumikire, Iye amalembanso zoyenera kuchitika ndipo amaloza antchito kuti agwire ntchitozo.

Pomaliza, awo amene Iye amawasankha ndi kuwaloza, Iye amawakhazikitsa. Yesu adamaliza ndi chiganizo, "Ndinakusankhani kuti mupite ndi kukabala zipatso." Iye ndiye Mbuye Wakholola, ndipo Iye ndi yemwe amatilamulira ife, "Mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse" (Marko 16:15). Kunena kwina, abusa enieni a Chipentekoste sadzisankha okha, sadziloza, kapena kudzitumiza okha. Koma, ndi osankhidwa, kulozedwa, ndi kutumizidwa ndi Mulungu. Gawo lathu ndi kumva liu lake, kudzipereka ku ulamuliro wake, ndi kumvera muyitano wake.

Mayitanidwe a Mulungu atha kufika munjira zosiyanasiyana. Akhoza kufika modabwitsa zedi, monga Samuele yemwe adamva mau a Mulungu oyitana dzina lake (1 Sam. 3:1-11). Kawirikawiri, komabe, kuyitana kwa Mulungu kumadza mwakachetechete komvekera mkati mwa munthu. Ichi chidachitika ndi mneneri Eliya. Mneneri sadamve mau a Mulungu mumphepo ya mphamvu, muchivomezi, kapena mu moto. Koma adamva mau a Mulungu ngati "kamphepo kayaziyazi" (1 Mafumu 19:12).

Kusuntha kwa kayaziyazi uku kawirikawiri kumatsagana ndi "kudziwa kwa mkati" kuti Mulungu akuyankhula. Nthawi ikamapita ichi chimakula, zotsatira zake umamva kufulumizitsidwa. Mnyamata Yesu nkutheka kuti adamva zoterezi pomwe adawauza makolo ake, "Kundiyenera Ine ndikhale m'zake wa Atate wanga" (Luka 2:49). Paulo adakamba za kufulumizitsidwa mkati za kwa Akorinto. "Pakuti chondikakamiza ndigwidwanacho", adalemba, "tsokaine ngati sindilalikira Uthenga Wabwino!" (1 Akorinto 9:16). Mneneri Mika adafotokoza za kutsimikizika kochokera kwa Mulungu mkati mwake: "Koma nine ndidzala nayo mphamvu mwa Mzimu ya Yehova.

Ndichiweruzo, ndi chamuna, kufotokozera Yakobo kulakwa kwake, ndikwa Israele tchimo lake" (Mika 3:8). Pamene tikuchitapo kanthu mwa chikhulupiriro ndi kumvera ku liu la Mzimu, kutsimikizika kumakula mpaka tidziwe

mosakayikanso kuti Mulungu watiyitana kuti tipereke miyoyo yathu kukulalikira uthenga wabwino.

Ubale Wamoyo

Pomaliza, mbusa wa Chipentekoste azikhala ndi ubale wopitirira, wamoyo ndi Mulungu. Kukumana ndi Mulungu kusamakhale kwa nthawi imodzi. Kukumana ndi Mulungu, ngakhale kutakhala kodabwitsa chotani, sikungagwirizize moyo wa Chikhristu. Ngakhale ophunzira oyamba, amene adakumana ndi Mzimu pa Tsiku la Pentekoste, adasoweka kudzadzidwanso mobwerezabwereza ndi Mzimu (Machitidwe 4:8, 31; 5;8).

Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kutakasa kuyenda ndi Mulungu kopitirira. Paulo adalemba kwa Akhristu atsopano ku Galatiya: "Ngati tili ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende" (Agalatiya 5: 25). Mukalata yomweyo, adawadzudzula iwo, "Kodi muli opusa otere? Popeza mudayamba ndi Mzimu, kodi tsopano mutsiriza ndi thupi?" (Agalatiya 3:3). Sizokwanira kungodzadzidwa, muyenera kukhala "wodzala ndi Mzimu" (Luka 4:1; Machitidwe 6:3; 7:5; 11:24). Yesu adalankhula za ubalewu ngati wokhalitsa, kapena wokhalamo mwa Iye (Yohane 15:4). Kukhala mwa Yesu kumatengera kukhala m'mau ake ndi m'chikondi chake (vv.7, 9). Kumatengeranso kusunga malamulo ake (v.10) ndi kukhala mwa Mzimu (1 Yohane 2:27; 4:13).

KUCHITA MOPHUNZIRA

Maluso ena sangathe kuphunziridwa kuchokera mmabuku. Munthu akhoza kuwerenga nkhani yokamba za kusambira; komabe, atha kukhala wopusa kudzigwetsera mmadzi ozama asadayambe kuphunzira maluso ake mmadzi osazama kwambiri. Chimodzimodzi ndi zoona ndi utumiki wa Chipentekoste. Pazokha, kuchuluka kwa maphunziro sikokwanira kukukonzekeretsani inu ku utumiki wa ubusa. Musadalowe mu utumiki muyenera kuchita mophunzira. Mutha kuphunzira mochita potenga nawo mbali mu utumiki.

Pa sukulu ya Baibulo ina yake kum'mwera kwa Afirika, woyembekerezedwa kukhala ophunzira amayenera kupereka "zikalata zofunsira malo pa sukulupo." Woyendetsa sukuluyi amagwiritsa chidziwitso chomwe amachipeza muzikalatazo kuwona ngati ofunsira malowo ndiwoyenera kudzayamba maphunziro pa sukuluyo. Pamodzi ndi mafunso okhudza moyo wa munthu ndi za maphunziro, ofunsira malo amayenera kulemba ndi manja awo za umboni wao. Mu umboni

wao ofunsira malo amafunsidwa kuti afotokoze zinthu zinayi izi: (1) anene momwe adamudziwira Khristu ngati Mpulumutsi wao (2) afotokoze za ubatizo wao wa Mzimu Woyera ndi momwe wakhudzira moyo wao (3) afotokozere za mayitanidwe awo ku utumiki (4) afotokoze momwe akhala akutengerapo gawo mu utumiki wa mpingo wao wapamalo.

Woyendetsa sukuluyi adati, "Timafunsa funso lomaliza chifukwa timakhulupirira kuti utumiki wochita ndi wofunikira zedi pa maphunziro autumiki." Ngakhale kuti maphunziro amkalasi ndi wofunikira, pawokha sangathe kukonzekeretsa inu ku utumiki wa ubusa. Muyenera kuphunzira mochita potenga nawo gawo lochitachita mu utumiki.

Simudzachita mwanzeru kuyesera kutsogolera mpingo ngati mbusa pokhapokha mutapeza luso mochita utumikiwo. Mutha kupeza lusoli mumpingo wapamalo pansi pa chitsogozo cha mbusa wokhwima, wodzadzidwa ndi Mzimu. Paulo adawuza Timoteo kuti woyang'anira akhale "wambiri yabwino kwa akunja" (1 Tim. 3:7). Madera anayi awutumiki wochita mu utumiki ndi kuchitira umboni, kulalikira ndi kuphunzitsa, kupereka, ndi kupemphera motere:

Kuchitira Umboni Mochita

Poyamba, pokonzekera utumiki wa ubusa, mukuyenera kudziwa kuchitira umboni mochita. Muyenera kukhala waluso pogawana uthenga wabwino ndi ena. Kuchitira umboni kumeneku ndi chotsatira chakubatizidwa ndi Mzimu Woyera, monga zakambidwa pamwambapa. Pokamba za Iye yekha, Yesu adati Mbusa "amakhala patsogolo pa nkhosa zake, ndipo nkhosa zimamutsatira iye" (Yohane 10:4). Monga mbusa wa Chipentekoste, chimodzimodzinso n'zoona ndi inu. Ngati mungakhale patsogolo pa nkhosa zanu kubweretsa miyoyo kwa Khristu, zidzatsatira. Koma ngati mulephera kuchitira umboni, chimodzimodzinso anthu anu.

Udindo wina wofananako ndi uwu wa mbusa wa Chipentekoste ndi wotsogolera mpingo wake mukudzala mipingo ya tsopanokumene mpingo wovekedwa mphamvu ndi Mzimu supezekako. Choncho ndi chinthu chofunikira kutengapo mbali kamodzi kapena kawiri podzala mpingo musanatenge utsogoleri wa mpingo wa pamalo. Izi zikhoza kuchitika ndi mpingo wa kumudzi kwanu, sukulu ya Baibulo yomwe mudapitako, kapena utumiki wina. Luso lophunzira

pochita ili lidzakuthandizani kudziwa kutakasa mpingo wanu omwe kudzala mipingo ina.[1]

Kuphunzira Kulalikira ndi Kuphunzitsa Mochita

Kuwonjezera apo, aliyense yemwe akufuna kukhala mbusa wa Chipentekoste akusoweka kupeza luso lochita la kulalikira ndi kuphunzitsa Mau a Mulungu. Chifukwa wina angatsogolere bwanji mpingo wa Chipentekoste mochitachita ngati iye sali ndi luso lolankhula Mau a Mulungu kwa ena? Paulo adakumbukutsa Timoteo kuti mbusa "akhoze kuphunzitsa" (1 Tim. 3:2). Adawonjezanso kulimbikitsa mwana wake m'chikhulupiriro kukonzekera kulalikira mau panthawi iliyonse (2 Tim. 4:2).

Njira imodzi yomwe mungapezere luso mochita la kulalikira ndi kuphunzitsa ndi kudzipereka nokha kuphunzitsa Sukulu ya lamulungu kapena kalasi ya Baibulo mu mpingo wa kwanu. Njira ina ndi yotsogolera gulu la limana. Munjira izi, mukhoza, pansi pa chitsogozo cha mbusa wanu, kuphunzira kuyika zonse pamodzi ndi kugawa mauthenga am'Baibulo. Njira inanso yabwino yopezera luso la kulalikira ndi kulalikira pa misonkhano ya pamtetete. Mutha kuchita ichi pobweretsa pamodzi gulu la mamembala ampingo okhulupirika ndi kupita kumisika ndi kwina kopezeka anthu pafupi ndi mpingo wanu kuti muchite misonkhano yofalitsa uthenga wabwino ya pamtetete.

Kupereka Kochita

Chachitatu, munthu amene akufuna kukhala mbusa wa Chipentekoste akhale ndi mbiri yokhulupirika ya chakhumi ndi kupereka moolowa manja ku ntchito ya Mulungu. Munthu wouma, woumira sangathe kuyimira Mulungu wowolowa, ndi wotsegula manja. Yesu adalimbikitsa ophunzira ake, "Munalandira kwaulere; patsani kwaulere" (Mateyu 10:8). Momwemonso, Paulo dalimbikitsa okhulupirira aChikorinto, "Khalani onditsanza ine, monga inenso nditsanza Khristu" (1 Akorinto 11:1). Pamene mamembala ampingo awona kuwolowa manja kwanu kodzadzidwa ndi chikhulupiriro, nawonso adzalimbikitsidwa kupereka

[1] Zinthu izi zafotokozedwa mwatsatanetsatane mu Mutu 37: "Kulalikira otayika" ndi Mutu 39: "Kudzala Mipingo Yatsopano."

mowolowa manja ku ntchito ya Mulungu, kudalira Iye kuti adzakwaniritsa zosowa zawo zonse (Afilipi 4:19). Zotsatira zake, ntchito ya Mulungu idzapindula.

Kupemphera Kochita

Pomaliza, iye wokhumba kukhala mbusa wa Chipentekoste akhale ndi luso lochita mu pemphero. Pemphero limayala maziko awutumiki wonse wa Chipentekoste. Kuchita pemphero kwa wina kumayamba ndi moyo wa pemphero wodziyika pa mwambo. Baibulo limatiuza kuti "Koma Iye anazemba, nanka m'mapululu, nakapemphera" (Luka 5:16). Kuti mukhale mbusa wa Chipentekoste wochitachita mukuyenera kuchita chimodzimodzi. Mukuyenera kupatula nthawi tsiku lililonse kukayanjana ndi Tate wanu wakumwamba.[2]

Mudzasowekanso kulumikizana ndi ena mu pemphero. Mukhoza kuchita ichi potengapo mbali mmagulu amapemphero, kupita kutali kukapemphera, ndi mapemphero ochezera usiku. Pochita izi, umadzikonzekeretsa wekha kupempherera ena. Madera ena awiri womwe mukuyenera kuphunzira mochita ndi kupempherera odwala ndi okanthidwa kuti achire ndiponso kupemphera ndi okhulupirira kuti adzadzidwe ndi Mzimu Woyera.

[2] Kuti mumve zambiri za moyo wodzipereka wa mbusa wa Chipentekoste, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero" ndi Mutu 15: Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu."

~ Mutu 2 ~

Munthu wa Mzimu

Mdziko lina la Chifirika mnyamata wina wachichepere adamva mayitanidwe a Mulungu pa moyo wake. Adawauza abusa ake za zimene amkamva. Abusa adazindikira mayitanidwe pa moyo wa mnyamatayu, ndipo adamutumiza iye ku nthambi ina ya mpingowu mtawuni ina yapafupi. Adamuuza mnyamatayo, “Ukuyenera kutukula mpingowu ndi kudzala mipingo ina m’dera ili.” Wodzazidwa ndi changu, mnyamatayu adasamutsira banja lake ku tawuniyo ndipo adadzikonzekeretsa yekha ku ntchitoyi. Adagwira ntchito molimbika ndikuchita kuthekera konse. Komabe adali ndi kupambana kochepa. Mnyamata wachichepere adati kwa iye yekha, “Ndikusowekera chidziwitso chokwanira ndi maphunziro.” Ndipo adalembetsa dzina lake ku sukulu ya Baibulo.

Ku sukulu ya Baibulo, mnyamata uja adaphunzira mau a Mulungu. Akupitirira kuphunzira, kulimbika kochuluka kumabwera. Adaphunziranso zachochitika cha m’Baibulo chotchedwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Mnyamatayu mwachangu adafuna Mzimu, ndipo posakhalitsa adadzazidwa, monga ophunzira zana limodzi kuwonjerapo makumi awiri pa Tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2:1-4).

Aphunzitsi ake adamuphunzitsa iye kuyenda mumphamvu ya Mzimu. Atabwerera ku mpingo wake, zinthu zidasintha. Tsopano amatumikira ndi mphamvu ndi chitsimikizo. Anthu adachiritsidwa ndi kumasulidwa, ndipo ambiri anabwera kwa Khristu. Chotsatira chake, mpingo udakula ndi kukhala wolimba.

Munthawi yochepa, udakhoza kudzala mipingo ina. Nkhaniyi ikuwonetsa kufunikira kwa mbusa aliyense wa Chipentekoste kuti akhale mwamuna kapena mkazi wa Mzimu.

Mutu womaliza unatambasula momwe mbusa wa Chipentekoste angakhalire munthu wa uzimu ndi waluso lophunzira mochita. M'mutu uwu titambasulako pa zinthu zimenezi. Udzafotokoza za chizindikiritso choyambirira cha mbusa wa Chipentekoste cha Mzimu ndi ntchito yake. Udzakambanso za kuyenda kwake ndi utumiki mwa Mzimu.

AMAZINDIKIRA MZIMU

Ngati inu, monga mbusa wa Chipentekoste, mungakhale munthu weniweni wa Mzimu, mukuyenera kuzindikira zinthu zinayi:

Mzimu Ndi Ndani

Choyamba, mukuyenera kuzindikira kuti Mzimu ndani. Akhristu ambiri lero, kuphatikizapo aChipentekoste, alibe maganizo omveka bwino akuti Mzimu Woyera ndi ndani. Ambiri molakwitsa amamuona Iye ngati mphamvu ina yake chabe yochoka kwa Mulungu. Mbusa wa Chipentekoste, komabe, ayenera kuzindikira ndi kuphunzitsa kuti Mzimu Woyera makamaka, ndi Mulungu. Iye ndi munthu wachitatu mu Utatu Woyera (Mateyu 28:19; 2 Ako. 13:14). Monga Atate ndi Mulungu, ndipo Mwana ndi Mulungu, Mzimu Woyera ndi Mulungunso. Monga Mulungu, Mzimu amaganiza (Machitidwe 15:28), amalankhula (Machitidwe 1:16), amatsogolera (Aroma. 8:16), ndiponso atha kumvetsedwa chisoni (Aefeso 4:30). Chifukwa Mzimu Woyera ndi munthu, wotsatira Khristu aliyense atha kukhala paubale ndi Iye (Yohane 14:16-18;2 Ako. 13:14). Kuwonjezera apo, monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kuzindikira ndi kuphunzitsa kuti Mzimu Woyera ndi Mzimu wa utumwi. Ndi membala uja wa Utatu amene, munthawi ya Mzimu, amanyamula cholinga cha Mulungu chowombola m'dziko lapansi. Komanso amapatsa mphamvu, amatakasa, ndi kutsogolera anthu a Mulungu kuti alumikizane naye mu utumwi (Machitidwe 1:8).

Momwe Mzimu Amagwirira Ntchito

Powonjezera kudziwa kuti Mzimu Woyera ndi ndani,mukuyenera kudziwa mmene amagwirira ntchito. Mzimu amagwira ntchito mwa anthu ndi kudutsira mwa anthu a Mulungu autumwi, mpingo, kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu

m'dziko. Adamupatsa mphamvu Yesu kuti akwaniritse ntchito yake (Luka 4:17-19; Machitidwe 10:38). Munjira yomweyo, adapereka mphamvu kwa otsatira a Yesu kuti akwaniritse ntchito yawo (Machitidwe 1:8; Yohane 14:12). Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kumvetsetsa bwino lomwe ndi kuphunzitsa zoonadi izi mokopa.[1]

Kuti mugwiritsitse za ntchito ya Mzimu m'nthawi ino, muyenera kuzindikira mfundo zitatu za m'Baibulo:

1. Utumiki wa Mulungu. Choyamba mukuyenera kuzindikira kuti Baibulo limamuonetsa Mulungu ngati Mulungu wa utumwi. Utumiki wake nthawi zina umatchedwa kuti *missio Dei*, ichi ndi Chilatini cha utumiki wa Mulungu. Utumiki wa Mulungu ndi kuombola, ndi kuyitanira kwa Iye yekha, anthu ochokera kumtundu uliwonse, ndi chilankhulo, ndi fuko lililonse pa dziko lapansi (Chiv. 5:9). Mpingo ulipo ngati chida chokwaniritsa utumiki.

Yesu adali ndi utumiki wa Mulungu m'maganizo ake pamene adapereka Utumiki Wake Waukulu: "Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la Atate ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera, ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulani inu" (Mateyu 28:19-20; Marko 16:15-16; Yohane 20:21).

Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kudzipereka nokha kuphunzitsa anthu a Mulungu za utumwi. Mukuyenera kuwaphunzitsanso iwo zagawo lawo pokwaniritsa utumwiwo.

2. Chikhalidwe Chautumiki cha Ubatizo wa Mzimu. Powonjezera kuzindikira za utumiki wa Mulungu, monga mbusa weniweni wa Chipentekoste, mukuyenera kumvetsetsa za gawo lofunikira la ubatizo wa Mzimu mukukwaniritsa utumiki. Muyenera kuzindikira kuti Mulungu amabatiza anthu ake mwa Mzimu wake kuwachititsa kuti akwaniritse utumiki wake (Luka 24:29). Yesu adayamba utumiki wake atapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera basi (Luka 3:21-23; 4:17-19). Iye akuyembekezera ophunzira ake kuchita chimodzimodzi lero (Machitidwe 1:4-8).

3. Kutakasira ku Utumiki. Chinanso, monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kuzindikira kuti, potsogolera anthu anu mu ubatizo wa Mzimu,

[1] Kuti mumve zambiri za nkhaniyi, onani Mutu 10: "Amalimbikitsa Choonadi cha Chipentekoste" ndi Mutu 11: "Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekoste."

mukuwakonzekeretsa ku utumiki wa mphamvu. Pamene Yesu adawalamulira akuphunzira ake, "Koma khalani inu m'mzinda muno, kufikira mwavekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba" (Luka 24:49), Iye amawakonzekeretsa ku utumiki umene udali patsogolo pawo (vv 47-48). Ndipo pamene Paulo adawafunsa ophunzira khumi ndi awiri aku Aefeso, "Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?" (Machitidwe 19:2), amafunsa zakukonzekera kwao kuti alumikizane ndi iye mu utumwi wolalikira mu Aefeso ndi konse ku Asiya (v.10).

Zikuyenera kukhala chimodzimodzi ndi ife lero. Tikuyenera kuzindikira kuti, powatsogolera anthu athu ku ubatizo wa Mzimu, tikuwakonzekeretsa kuti akachitire umboni wamphamvu ya Mzimu, kudzala mpingo, ndi utumwi.

Kumasulira Buku la Machitidwe

Chachitatu, monga mbusa weniweni wa Chipentekoste muAfirika, mukuyenera kugwiritsitsa chikhalidwe cha utumiki ndi cholinga cha buku la Machitidwe. Chinthu chimodzi chomwechimasiyanitsa aChipentekoste kwa anthu oti siaChipentekoste ndi momwe gulu lililonse limamasulira buku la Machitidwe. Gulu lomwe silaChipentekoste kwenikweni amaona Machitidwe ngati mbiri ya momwe Mpingo udayambira ndi kuchitira utumiki wake. Mkuganiza kwao, Machitidwe akufotokoza momwe Mulungu adagwirira ntchito nthawi imeneyo kumeneko, kalekale. A Chipentekoste, komabe, amaona buku la Machitidwe ngati dongosolo lomaliza la momwe Mulungu akufunira kugwirira ntchito mkati mwa Mpingo ndi kudzera mumpingo pano ndiponso tsopano, m'nthawi ino.

Mbusa wa Chipentekoste amazindikira kuti buku la Machitidwe ndi loposera pa buku la mbiri yakale. Ndi dongosolo lowuziridwa ndi Mulungu la utumiki wa m'nthawi yotsiriza. Mu Machitidwe, Mzimu Woyera wapereka kwa Mpingo chitsanzo, njira, ndi dongosolo lokwaniritsira utumiki wa Mulungu. Dongosolo limeneli lanenedwa mofupikitsidwa mulonjezo lomaliza la Yesu ku Mpingo: "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko" (Machitidwe 1:8).

Ndime iyi ikuonetsa dongosolo la umboni-wamphamvu limene likubwerezedwa m'bukuli. Popanda choletsa, kutsanulira konse kwa Mzimu mu Mchitidwe kudatsatiridwa ndi umboni-wamphamvu ya Mzimu. Kugwiritsa

mfundoyi ndi chofungulira kuzindikira kwanu kwa buku la Machitidwe ndi kutakasa mpingo wanu kuti uzichita utumuki wamphamvu-ya Mzimu.

Chimene Chimatanthauza Kuti Wa Chipentekoste

Pomaliza, monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kukhala ndi kuzindikira kuti chimatanthauzanji kuti wa Chipentekoste. Chipentekoste chenicheni ndi choposera njira yolambirira kapena kuphunzitsidwa za mphamvu ya zauzimu. Mulungu adadzutsa Mpingo wa Chipentekoste ngati mayendedwe ammasiku otsiriza autumwi amphamvu ya Mzimu. Mbusa weniweni wa Chipentekoste choncho adzipereke kutsatira dongosolo la utumiki lomwe lidayalidwa ndi Yesu mmabuku authenga wabwino ndipo udatengeredwa ndi atumwi ndi ophunzira ena m'buku la Machitidwe. Iye wadzipereka kumachitidwe azinthu anayi am'Baibulo:

1. Uthenga Omwewo. Choyamba, mbusa weniweni wa Chipentekoste ndiwodzipereka mokhulupirika kulalikira uthenga womwewo monga adachitira atumwi ndi alaliki mbuku la Machitidwe. Uthenga umenewo ndi uthenga wabwino. Ukuwonetseredwa mu utumiki wa Filipo amene "adatsikira ku mzinda wa Samariya, nawalalikira iwo Khristu" (Machitidwe 8:5; fanizilani v.12). Kudutsa mbuku lonse la Machitidwe, Mpingo sunagwedezeke kupatuka pa kulalikira uthenga wa imfa yochotsa machimo ya Yesu ndi kuuka kwake (fanizilani 2:22-24; 3:15; 4:10-12). Powonjezera, adayitana anthu kawirikawiri kuti alape ndi kukhulupirira uthenga wabwino (fanizilani 2:38; 16:31; 20:21; 26:20). Tikuyenera kuchita chimodzimodzi lero.

2. Utumiki Womwewo. Chachiwiri, mbusa weniweni wa Chipentekoste ndiwodzipereka kukutsatira utumiki womwewo monga udachitira Mpingo mubuku la Machitidwe. Monga zanenedwa pamwambapa, utumikiwu wafupikitsidwa bwino mu Machitidwe 1:8, pomwe Yesu adati, "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga…kumalekezero ake a dziko." Buku la Machitidwe likuwonetsa Mpingo umene ukupita patsogolo, kulowa mmadera atsopano mopitiriza, ndi kulalikira uthenga wabwino mu mphamvu ya Mzimu. Monga mbusa woona wa Chipentekoste, mukuyenera kutsogolera mpingo wanu kuchita chimodzimodzi.

3. Zochitika Zomwezo. Chachitatu, mbusa weniweni wa Chipentekoste amapititsa patsogolo zochitika zauzimu zomwezo monga adachitira atumwi mbuku la Machitidwe. Zochitika zomwezo zikuphatikizapo kutembenuka

kosintha moyo (fanizilani Machitidwe 2:41; 8:5-6; 9:1-8), ubatizo womiza m'madzi (fanizilani 2:41; 8:13, 36-38; 9:17-19; 16:33), ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chizindikiro cholankhula malilime ena (fanizilani 2:4; 10:44-46; 19:6), zozwiza za machiritso (fanizilani 3:1-10; 5:12-16; 20:7-12), ndi zozwiza zamamasulidwe kwa wogwidwa ndi ziwanda (fanizilani 8:7; 16:16-18). Ndi muyeso womwewu, mbusa wa Chipentekoste adzakana chozizwa chilichonse kapena chochitika cha uzimu chosagwirizana ndi Malembo.

4. Njira Zomwezo. Pomaliza, mbusa wa Chipentekoste adzagwiritsa ntchito njira zomwezo adagwiritsa ntchito atumwi ndi ena m'buku la Machitidwe. Njira zimenezi zikuphatikizapo malalikidwe a uthenga wabwino odzodzedwa a Mzimu obweretsa kutsutsa kozama, chikhulupiriro, ndi kulapa (fanizilani Machitidwe 2:14-41; 8:13). Mbusa wa Chipentekoste amayembekezeranso Mulungu kukwaniritsa mau ndi zizindikiro, komanso zozwizwa zamalankhulidwe, machiritso, ndi mamasulidwe (fanizilani 5:12-16; 10:44-47; 14:6-10).[2]

Kuwonjezera apo, mbusa weniweni wa Chipentekoste amayembekezera Mzimu Woyera kumtsogolera iye mu utumiki (fanizilani Machitidwe 8:29; 10:9-20; 16:6-10). Chitsogozo ichi chitha kubwera mkukakamizidwa kwa mkati (fanizilani 8:29; 10:19), maloto (fanizilani 2:17; 16:9), ndi masomphenya (fanizilani 9:10-16; 10:9-20). Njira yayikulu ya kulalikira yomwe idagwiritsidwa ndi atumwi mbuku la Machitidwe inali yodzala mipingo ya utumwi ya mphamvu ya Mzimu imeneikadafikira kumadera ozungulira ndi uthenga wa Khristu.[3]

AMAYENDA NDI MZIMU

Mbusa wa Chipentekoste asangozindikira kuti Mzimu ndi ndani, ndi momwe amagwirira ntchito, iye akuyenera kuphunzira kukhala pansi pa chitsogozo cha Mzimu. Paulo adabetchera okhulupirira atsopano ku Galatiya, "Mudayamba ndi Mzimu, kodi tsopano mutsiriza ndi thupi?" (Agalatiya 3:3). Iye amawakumbukutsa iwo momwe adayambira kuyenda kwao kwa Chikhristu. Adayamba ndi kubadwa mwa Mzimu ndi kudzadzidwa ndi Mzimu.

[2] Mukafuna zambiri pa nkhani zimenezi, onani Mutu 16: "Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu" ndi Mutu 21: "Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu."

[3] Mukafuna kumva zambiri za kudzala mipingo yodzazidwa ndi Mzimu, onani Mutu 39: "Kudzala Mipingo Yatsopano."

Tsopano,adayenera "kuyenda motsatirana ndi Mzimu" (5:25). Ichi chidzikhala cholinga cha mbusa aliyense wa Chipentekoste mu Afirika.

Njira ziwiri zofunikira zomwe mungachitire izi ndi popemphera mu Mzimu ndi potakasa chipatso cha Mzimu, motere:

Pemphero la mu Mzimu

Baibulo limalankhula za mitundu ya pemphero, kuphatikiza kupembedzera, chofuna, kuvomereza, chopempha, kulambira, kuyamika, ndi ena ambiri. Pemphero la mu Mzimu, komabe,ndiloyenera polimbikitsa kuyenda kodzadzidwa ndi Mzimu. Paulo akuyankhula za mtundu uwu wa pemphero mu Aefeso 6:18. Komanso, mu Aroma 8:26, akufotokoza momwe pemphero la Mzimu limagwirira ntchito. "Mzimu athandiza kufooka kwathu; pakuti chimene tizipempha monga chiyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka." Ngakhale kuti pemphero la mu Mzimu litha kukhala pemphero lililonse loyambitsidwa, lodzodzedwa, ndi lotsogoleredwa ndi Mzimu (1 Ako. 14:14-15). Monga Mbusa wa nzeru wa Chipentekoste, muyenera kugwiritsa ntchito chida ichi champhamvu kawirikawiri (2 Ako. 10:4-5).[4]

Chipatso cha Mzimu

Njira ina yofunikira yolimbikitsa kuyenda kwanu kwa uzimu ndi kutakasa chipatso cha Mzimu. Paulo adawona kuti chipatsochi ndi "chikondi, chimwemwe, mtendere, chipiriro, kukoma mtima, ubwino, kukhulupirika, chifatso, ndi chiletso (Agalatiya 5:22-23).

Monga mbusa wa Chipentekoste, musangodziwa mphamvu ya Yesu yokha, moyo wanu uzionetsa chikhalidwe chake. Mphatso zokha popanda chipatso zimakhala "mkuwa woomba, kapena nguli yolira" (1 Ako. 13:1). Ambiri amene sangabweretsedwe kwa Khristu kudzera muchiwonetsero cha mphamvu atha kukopedwa ndi ntchito za chikondi. Mutha kutukula chipatso cha uzimu mmoyo wanu poyenda mu Mzimu (Agalatiya 5:16) ndi kukhala mwa Khristu (Yohane 15:4).

[4] Mukafuna kumva zambiri za Moyo wapemphero wa mbusa wa Chipentekoste, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

AMATUMIKIRA MU MZIMU

Yesu adati, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chake Iye anandidzodza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino" (Luka 4:18). Potsatira chitsanzo cha Ambuye, Paulo adafotokozera utumiki ngati "chiwonetsero cha mphamvu ya Mzimu" (1 Ako. 2:4). Chimodzimodzinso, inu, monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kudzipereka nokha konyamula utumiki wanu mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Ngati Paulo, mukuyenera kuyesetsa kukhala mtumiki wakutha ntchito mwa Mzimu (2 Ako. 3:6).

Chifukwa cha ichi, mudzikhala tcheru kumagwiridwe a ntchito a Mzimu (kulephera kapena kugwira ntchito) mmoyo ndi mu utumiki, ndiponso pakati pa anthu omwe mukuwatumikira. Muyenera kukaniza mtundu uliwonse wa maonekdwe achipembedzo opanda mphamvu ya Mzimu ndi kupezeka kwake (2 Tim. 3:5), ndiponso muyenera kutetezera chiphunzitso chorama, chochitika, ndi luso lochita (fanizilani Yuda 1:3).[5] Njira zitatu zomwe mungachitire izi ndi potsatira kudzodza kwa Mzimu, kufuna chitsogozo cha Mzimu, ndi kufunitsitsa mphatso za Mzimu.

Kutsatira Kudzodza kwa Mzimu

Monga mbusa weniweni, mukuyenera kukhala ndi chidwi kutsatira kudzodza kwa Mzimu. Nthawi zonse muzifuna kulalikira, kuphunzitsa, ndi kutumikira pansi pa chiwonetsero cha kupezeka kwa Mulungu. Ndiye kuti, mukuyenera kupemphera ndi kudzipereka kwa Mzimu, kuyembekezera Iye, kukupatsani mphamvu kuti mutumikire ndi mphamvu ndi ulamuliro wochuluka. Kudzodza kwa Mzimu kudzakopa ngakhale mitima yolimbitsitsa, kuyichititsa kuti itembenukira kwa Mulungu ndi kunena, "Yesu ndi Ambuye!"

Kufuna Chitsogozo cha Mzimu

Chinanso, mukuyenera kudalira Mzimu wa Ambuye kukutsogolerani inu mu utumiki. Ichi ndi chimene amachita Yesu ndi ophunzira ake. Mbusa wanzeru wa Chipentekoste amazindikira kuti Mzimu Woyera ndi wotsogolera wa utumiki wa Mulungu. Iye yekha amazindikira zosowa ndi zofunikira za utumiki. Mzimu adatsogolera Filipo kwa Msungichuma wa ku Ayitiopia (Machitidwe 8:26-38),

[5] Mutha kuwerenga zambiri za utumiki wamphamvu ya Mzimu mu Mutu 21: "Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu."

Petro kunyumba ya Koneliyo (Machitidwe 10:9-25), ndi Paulo ndi gulu lake utumwi kupita ku madzulo kwa Asiya (Machitidwe 16:6-40). Adzachita chimodzimodzi ndi ife lero. Tikakhala otsegukira ndi atcheru ku liwu lake, Mzimu wa Ambuye adzatitsogolera ife ku ntchito ya Khristu.

Kufunitsitsa za Mphatso za Mzimu

Paulo adalimbikitsa okhulupirira kuti "funitsitsani mphatso zauzimu" (1 Ako. 14:1). Monga Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste, mukuyenera kumvera langizo la mtumwi potakasa machitachita amphatso zauzimu mmoyo wanu ndi mmoyo wa mpingo umene mukutsogolera. Ndikudzera mu mphatso zimenezi momwe kudzodza kumene kunalandiridwa pa ubatizo wa Mzimu kumamasulidwa mu utumiki. Paulo akukamba za ntchito za mphatso mu 1 Akorinto 12-14. Luka akuchitanso chimodzimodzi mu buku la Machitidwe. Paulo akulunjika pa machitachita a mphatso mu mpingo umene wasonkhana polambira (1 Ako. 14:23-26), pamene Luka akuonetsa momwe mphatso zimagwirira ntchito kutsogolo kwenikweni kwa kulalikira kwa otayika ndi podzala mpingo.[6]

Mu uthenga wake womaliza wa kwa Timoteo, Paulo adalimbikitsa mwana wake m'chikhulupiriro kuti "akoleze mphatso ya Mulungu" imene idali mwa iye kudzera mukuyikidwa manja ndi atumwi (2 Tim. 1:6). Amamulimbikitsa Timoteo kukhala munthu wa Mzimu. Mbusa aliyense wa Chipentekoste mu Afirika akhozakuchita bwino potsatira uphungu wa Paulo kwa Timoteo. Akuyenera kulondera "chosungitsa chokomacho" cha Mzimu Woyera chomwe chayikizidwa kwa iwo (2 Tim. 1:14). Pochita ichi, aziwonetsetsa kuti akukhalabe odzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi odzipereka ku utumiki wa Mulungu. Ndiponso aziyesetsa kupereka mautumiki awo mu mphamvu ndi m'kudzodza kwa Mzimu Woyera.

[6] Mphatso za Mzimu zafotokozedwa kwambiri mu Mutu 21: "Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu." Mphatso zimenezi zasanjidwa ndi kutambasulidwa mu Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

~ Mutu 3 ~

Munthu Wakhalidwe Labwino

MNENERI WAMANGIDWA CHIFUKWA CHOPEREKA PAKATI KWA ATSIKANA ACHICHEPERE.” Nkhani yosokonezayi idaonekera mu tsamba losindikiza nkhani la kumwera kwa Afirika. Nkhaniyi idapitilira kufotokozera momwe atsikana achichepere, ena azaka pafupifupi khumi ndi zinayi, adapatsidwira pakati ndi “mneneri wa Chikhristu” wodziwika bwino. Atsikanawa adapitira limodzi kwa adindo kukamuneneza mlaliki wakhalidwe lovundayo. Mwatsoka ilo, monga momwe zidali kukhalira ndizolakwitsa zina m’mbuyomo, mpingo udachititsidwa manyazi, ntchito ya Mulungu kudetsedwa, komanso kunyozetsa dzina la Yesu.

Ngakhale kuti zinali choncho, sikuti ndi machimo owonekera kugulu otere omwe amabwezera m’mbuyo kayendedwe ka mpingo ayi; koma ang’onoang’ono omwe ndiobisika. Akani adachimwa mseri, koma tchimo lake lidakhudza gulu lonse (Yoswa 7:1-12). Momwemonso, mphulupulu zamseri za mbusa zingathe kuononga mpingo onse. Chifukwa chakusowa khalidwe kwawo, atumiki ambiri a Mulungu achititsa manyazi ntchito ya Mulungu mpaka kudzichotsa okha mu utumiki.

Khalidwe labwino ndi maziko amene utumiki wa Chipentekoste wochitachita umamangidwapo. Popanda maziko amenewa, zonse zidzagwa ndi kulephera. Utumiki okhalitsa sungamangidwe pa luso, mankhwala a zitsamba, mmene munthu aliri, maphunziro apamwamba, kapena kudzodza kwapamwamba.

Ukuyenera kuti umangidwe pa maziko olimba a khalidwe labwino. Pamwamba pa zonse, anthu a Mulungu azikhala nkuthekera komudalira mbusa wao.

KUFUNIKA KWA KHALIDWE

Mbusa wa Chipentekoste azikhala munthu wakhalidwe lapamwamba. Paulo adamulembera Timoteo yemwe ankatumikira ngati mbusa wampingo waku Aefeso, kumulimbikitsa kuti azikhala moyo wachitsanzo:

"Ndipo kuyenera woyang'anira akhale wopanda chilema, mwamuna wamkazi mmodzi, wodzisunga, wodziletsa,wolongosoka, wokonda kuchereza alendo, wokhoza kuphunzitsa; wosati woledzera, kapena womenyana ndeu; komatu wofatsa, wopanda ndeu, wosakhumba chuma"(1 Timoteo 3:2-3).

Paulo adalimbikitsanso Tito zokhudza khalidwe la mbusa:

"Pakuti woyang'anira ayenera kukhala wopanda chilema, ngati mdindo wa Mulungu; wosati waliuma, wosapsa mtima msanga, wosati wachiwawa, wopanda ndeu, wosati wachisiriro chonyasa; komatu wokonda kuchereza alendo, wokonda zokoma, wodziweruza, wolungama, woyera mtima, wodziletsa." (Tito 1:7-8)

Onani m'mene mu mindandanda yonseyi Paulo akulankhulira zokhudza khalidwe poyambirira osati kuthekera. Ngakhale kuti kuthekera ndikofunikira kwa mbusa wa Chipentekoste, khalidwe liri pamwamba pa zonse.

TANTHAUZO LA KHALIDWE

Kodi mau oti khalidwe atanthauzanji? Khalidwe limalankhula za machitidwe a munthu. Ndi munthu amene ife tili mkati mwathu. Kwa m'Khristu, khalidwe ndiko kufanana naye Yesu. Khalidwe limalosera machitidwe a munthu (kapena kuyankhapo pa zinthu) akafinyika. Ndi chimene ife tili malo amene aliyense sakutha kutiona. Mau ena a khalidwe ndi ungwiro. Ungwiro umalankhula za kukhala bwino mu uthunthu wonse kapena wamphumphu.

Monga abusa a Chipentekoste, tizikhudzika kwambiri ndi khalidwe lathu osati mbiri yathu. Izi zili chomwechi chifukwa mbiri ndi kaganizidwe ka anthu za mmene ife tiliri, pamene khalidwe lathu ndi chenicheni chomwe ife tili. Kumbukirani chenjezo la Mulungu kwa Samuele pamene adayesedwa kuti adzodze mkulu wake wa Davide kuti akhale mfumu ya Israeli. Mneneri adati, "Pakuti munthu ayang'ana chooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana mumtima" (1 Samuele 16:7). Samuele adadzodza Davide monga mfumu chifukwa

adali munthu yemwe adasankha kukondweretsa Mulungu (1 Sam. 13:14; Machitidwe 13:22).

Khalidwe la umulungu limaonekera mu ngodya zitatu za moyo ndi machitachita a mbusa wa Chipentekoste munjira zotsatirazi:

Kuona Mtima

Mbusa weniweni wa Chipentekoste amasankha kutsatira mapazi a Yesu, "amene sanachite tchimo, ndipo m'kamwa mwake sichinapezedwa chinyengo" (1 Petro 2:22). Iye amakhala owona mtima mkalumikizanidwe ndi anthu ena. Mukunena kwina, mbusa waChipentekoste amakana kunama-ngakhale pamene zikuoneka kuti bodza ndiyo njira yokhayo yosapweteka yotulukira mu nyengo yovuta. Paulo adalimbikitsa Akhristu aku Aefeso kuti "mwa ichi, munataya zonama, lankhulani zoona yense wina ndi mzake" (Aefeso 4:25).

Monga mbusa wa Chipentekoste, yesetsani kukhala ndi mbiri mudera lanu kuti nthawi zonse mukalankhula, anthu azidziwa kuti akumvetsera choonadi. Ngati sangakukhulupilireni mukayankhula kumsika, akukhulupirirani bwanji mukalankhula pa gome? Mudziwike monga munthu amene nthawi zonse "(amalankhula) choonadi mwachikondi" (Aefeso 4:15).

Ungwiro pa Ndalama

Monga mbusa wa Chipentekoste wokhulupirika, muzikhala woona mtima mu kalumikizanidwe kanu, ndipo muyenera kukhala wokhulupirika kwambiri mu zonse zokhudza kayendetsedwe ka chuma. Izi zikuphatikizapo zachuma zanu ndi Mulungu, mpingo, ndi iwo akunja kwampingo. Mumachita izi podziwa kuti Mulungu akuona. Ndipo, pamwamba pa zonse, mukufuna kumusangalatsa Iye. Choncho, mumakana kumubera Mulungu zakhumi ndi zopereka zanu (Malaki 3:8).

Abusa ena amalamula kuti mamembala awo azipereka chakhumi chawo ku mpingowo pamene iwo eni sapereka. Pakuchita izi, sikuti amangomubera Mulungu ayi, amaonetsera chinyengo cha mitima yawo. Ngati ndinu munthu wotere, lapani ndipo chitani zimene mukudziwa kuti ndi zolondola (onani Machitidwe 26:20).

Kuonjezera apo, mukhale aulemu pakayendetsedwe kachuma cha mpingo. Poti ndinu mbusa sizikukupatsani chilolezo chogwiritsa ntchito ndalama za

mpingo m'mene mwafunira ayi. Muzisamalira bwino lomwe zopereka zonse za mpingo. Ndipoonetsetsani kuti ndalamazo zikugwira ntchito yokhayo yomwezifunikira kutero. Mwachitsanzo, musagwiritse ntchito ndalama zoperekedwera ntchito yautumwi kugulira galimoto, kapena ndalama zofalitsilira uthenga wabwino kukonzetsera nyumba yopemphereramo. Komanso, musayelekeze kutenga ndalama zopatsidwa kuti zithandize osauka, ndipo monga Yudasi yemwe ankasololamo m'thumbamo, m'kugwiritsira ntchito zakumtima kwanu (onani Yohane 12:6).

Kuwonjezera apo, monga mbusa wa Chipentekoste wokhulupirika, muzikhala okhulupirika pakachitidwe kanu kokhudza chuma ndi anthu akunja kwa mpingo. Muzidziwika monga munthu waungwiro wapamwamba kwambiri. Musamabe, kunamiza ena, kapena kulephera kubweza ndalama iliyonse yomwe munabwereka. Kuchita zosemphana ndi izi ndiye kuti mpingo udzayipitsidwa komanso anthu atha kusiya kutsata njira ya Yesu.

Kupewa Chiwerewere/Chigololo

Monga mbusa wa Chipentekoste, sikuti muzingokhala wokhulupirika mukalumikizanidwe kanu, ndi kuona mtima pazachuma zanu, mukuyeneranso kudzipatsa ulemu kwa iwo osiyana nawo chilengedwe nthawi zonse. Muzikhulupirika ku malonjezo anu a banja ndi "kukana choipa cha mtundu uliwonse" (1 Atesa. 5:22).

Muziyesa "akazi aakulu monga amai; akazi aang'ono ngati alongo, m'kuyera mtima konse" (1 Tim 5:2). Pakutero, muzionetsetsa kuti simuli panokhanokha ndi mkazi amene sali mkazi wanu. Muzionetsetsanso kuti mukupewa kuyanjana kwa maimvaimva ndi mkazi aliyense yemwe si wanu kudutsira mu kulankhulana ndi machitidwe osasamala. Abusa a akazi naonso akuyenera kusamalitsa zimenezi pakachitidwe kawo ndi amuna.

Monga mtumiki wa Khristu, mugwiritsitse kwambiri zomwe Paulo adalankhula: Koma dama ndi chidetso chonse, kapena chisiriro, zisatchulidwa komwe mwa inu, monga kuyenera oyera mtima" (Aefeso 5:3).

MAKHALIDWE ENA OFUNIKIRA

Monga oyimirira Mulungu, mufunitsitse kukhala ndi makhalidwe ena a umulungu. Maonekedwe asanu omwe afunikira kuwatchula ndi kulimba mtima, kudalirika, kudzichepetsa, chifundo, ndi kukoma mtima, ndipo zili motere:

Kulimba Mtima

Kulimba mtima ndi mphamvu zakhalidwe lochita zolondola ngakhale pali chiopsezo, zovuta, kapena choopsa. Ndi kulimba mtima kokhala kadziwotche, kuyimabe pa chinthu chomwe ndi chabwino, ndi kukhulupirira Mulungu pamene pakuoneka kuti kulibe kolowera. Nelson Mandela adalemba mu mbiri ya moyo wake, "Ndidaphunzira kuti kulimba mtima sikudali kusapezeka kwa mantha, koma kuwagonjetsa. Munthu wolimba mtima si iye yemwe sakhala ndi mantha, koma iye amene amagonjetsa manthawo."

Kulimba mtima ndi mau otsutsana ndi mantha. Mantha ndi mwana wa kukhudzika kwa iwe mwini kowonjezereka; kulimba mtima kumabadwa pokhudzika ndi ena. Mantha amachititsa kuti munthu asachite kapena kunena cholondola; kulimba mtima kumamupanga munthu kuti akhalebe pa choonadi pomwe pali choopsa. Mose adali wolimba mtima pamene adayima pamaso pa Farao kulamula kuti mfumu ya Aejipito imasule anthu a Mulungu (Ekso. 5:7). Yesu adalimba mtima pamene adagonjera modzichepetsa ku manyazi ndi ululu wa mtanda (Aheb. 12:2). Ndipo Stefano adalimba mtima pomwe adauza atsogoleri achiYuda kuti iwo adapha Mesiya wao (Mach. 7:51-52).

Ife tikadzamvera Mzimu Woyera wokhala mkati mwathu, Iye adzatipatsa kulimba mtima komwe timafuna kuti tiyime mwa Khristu ndikulengeza dzina lake kwa onse. Pamene adaopsezedwa, Petro ndi Yohane adapemphera, "Ndipo tsopano Ambuye, penyani mau ao akuopsa, ndipo patsani kwa akapolo anu alankhule mau anu ndi kulimbika mtima konse." Poyankha pemphero lawo, Mulungu adawadzadza ndi Mzimu Woyera, ndipo "adalankhula mau a Mulungu molimbika mtima" (Mach. 4:29-31). Monga mbusa wa Chipentekoste, funitsitsani kukhala muchidzalo cha Mzimu Woyera ndi wodalira Mulungu kuti akupaseni kulimbika mtima komwe mumafuna kuti mukwaniritse mayitanidwe anu mokhulupirika.

Kudalirika

Kuonjezerapo, muzikhala odalirika monga kapitawo kapena woyang'anira mpingo wa Yesu. Ambuye azikudalirani kwathunthu inuyo (Tito 1:7; 1 Pet. 4:10). Paulo adati, "komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika" (1 Ako. 4:2). Moyo uzionetsera makhalidwe oterewa monga kudalirika, kusunga nthawi, kupilira, ndi kutsimikizika. Makhalidwe otere ndi zipatso za kuyenda ndi chidzalo cha Mzimu (Agal. 5:22).

Paulo adawauza akuluakulu aku Aefeso, "Tadzichenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuyikani woyang'anira, kuti muwete Mpingo wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi wa Iye yekha" (Mach. 20:28). Monga abusa, Mulungu watidalira ndi miyoyo ya amuna ndi akazi. Ndipo tsiku lina tidzayankha mlandu kwa Mulungu wokhudzana ndi kukhulupirika kwathu pankhaniyi (Aheb. 13:17). Yakobo akuchenjeza, "Musakhale aphunzitsi ambiri, abale anga, podziwa kuti tidzalangika koposa" (Yak. 3:1).

Kudzichepetsa

Monga wotsanzira Khristu, mbusa wa Chipentekoste akhale wodzichepetsa (Aef. 5:1). Yesu adauza ophunzira ake, "Koma aliyense amene akafuna kukhala wamkulu mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo aliyense amene akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu: monga Mwana wa Munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la anthu ambiri" (Mat. 20:26-28).

Ndizosokoneza kwambiri kumuona mbusa wa Chipentekoste ali odzadzidwa ndi kunyada ndi kudzikundikira, kulamula kutiazitumikiridwa ndi ena m'malo mowatumikira. Machitidwe otere ndiwosiyana kwambiri ndi zomwe Ambuye wathu adaonetsa. Paulo adawalembera Akhristu aku Filipi, "Mukhale nao mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu, ameneyo, pokhala nawo maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofanana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe akapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda" (Afil. 2:5-8). Mtsogoleri wamwano amafuna kutumikiridwa; mbusa wa umulungu amakondwera mkutumikira ena modzichepetsa.

Chifundo

Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kukhala munthu wachifundo. Chifundo ndiko kuonetsera machitachita a chikondi. Chimaonekera pokhudzika ndi iwo omwe ali ndi chosowa. Ndi kuonetsera poyera kwa mtima wodzala ndi chikondi cha Mulungu. Baibulo limati, ponena za Yesu, "Koma iye poona makamuwo, anagwidwa m'mtima ndi chisoni chifukwa cha iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkhosa zopanda mbusa" (Mat. 9:36).

Chifundo cha Yesu chidamutakasa iye kuti asamalire zosowa za anthu zauzimu ndi kuthupi. Monga oweta nkhosa za Mulungu, titengereko kukhudzika kwa chikondi uku kwa anthu Ake, ndi iwo omwe sadamulandire Khristu. Chifundo chidzatichititsa kuti tisamalire ena munthawi ya kusowa kwao, ndipo chidzatisuntha kuti tilalikire uthenga wabwino kwa onse.

Monga anthu a Mulungu, kuyendabe kwathu ndi Mzimu kutitakase kuti tikonde ndi kusamalira ena. Paulo adati, "Chikondi cha Mulungu chinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife" (Aro. 5:5). Mwa anthu onse, ife amene timati tili ndi chidzalo cha Mzimu wa Khristu tizionetsera chifundo cha Yesu kwa ena.

Kukoma Mtima

Maonekedwe ofunikira akhalidwe kwa mbusa wa Chipentekoste wamachitachita, ndi kukoma mtima. Pokhala chotsatira chakulandira chidzalo cha Mzimu Woyera pa Tsiku la Pentekoste, okhulupirira oyamba adali odzala ndi mzimu wa kukoma mtima. Pokamba za iwo, Baibulo limati, "Ndipo onse akukhulupirira anali pamodzi, nakhala nazo zonse zodyerana. Ndipo zimene anali nazo, ndi chuma chao, anazigulitsa, nazigawira kwa onse, monga momwe yense anasowera" (Mach. 2:44-45). Momwemonso, monga mbusa wodzala ndi Mzimu, muzichita changu pogawana nawo iwo omwe ndi osowa. Muzikhala owolowa manja kwa Mulungu, mpingo, ndi ena omwe ndi osowa.

Pamene ankawatumiza khumi ndi awiriwo, Yesu adawauza, "Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, tulutsaniziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere" (Mat. 10:8).Kukoma mtima kotereku ndi kopatsirana. Pamene anthu aona kumasuka kwa mbusa wao, naonso adzalimbikitsika ndi kutsekula mtima ndi malo ena osungira ndalama nawolowa manja. Chikhalidwe ichi cha kukoma mtima chidzakhudza mpingo mwamphamvu, dera lozungulira, ndi mafuko a padziko lapansi komalizira.

KUMANGA KHALIDWE

Funso limakhala lakuti: Kodi Mbusa wa Chipentekoste angamange bwanji khalidwe la umulungu lomwe lakambidwa m'mwambamu? Timachita izi potsatira chitsanzo cha Yesu. Iye ndiye kalilore wa moyo ndi utumiki wathu. Yohane adalemba kuti, "Iye wakunena kuti akhala mwa Iye ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayenda Iyeyo" (1 Yoh. 2:6).

Mu mau a Paulo, "tiyenera kudziveka Khristu tokha" (Ako. 3:12-17; Aroma 13:14). Pamene Yesu adalamulira ophunzira ake, "Tsatani ine" (Marko 4:19), adali kuwauza kuti amuone iye ndi kuyika miyoyo yawo monga wake. Pakuchita zimenezi, iwo adasandulika m'chifanizo chake (Arom. 8:29; 2 Ako. 3:18). Pang'ono ndi pang'ono, miyoyo yawo ikankhala ngati wake. Ndi mphamvu ya Mzimu, adayamba kukhala monga iye adakhalira, kuganiza monga iye adaganizira, ndi kukonda monga iye adakondera (2 Pet. 1:3-4). Ngati mufuna mukhale mbusa wa zotsatira wa Chipentekoste, funitsitsani kukhala ngati Yesu.

Pamene khumi ndi awiriwo adatsatira Yesu, iwo adakhala oposera chomwe adali mmbuyo mwake. Komabe, pakumutsatabe iye, adakhala asodzi a anthu monga momwe Mbuye wao adaliri. Mkunena kwina, iwo adavala khalidwe lake la Yesu. Ophunzira a Baibulo nthawi zina amayitcha ndondomeko iyi kuti kuwumbidwa kwauzimu.

Tisayerekezere kuganiza kuti tingathe kufikira khalidwe longa la Yesu mukuyesetsa kapena mphamvu zathu ayi. Tiyenerakuthandizidwa ndi Mulungu. Tingathe kupeza thandizo lake pochita mwambo utatu wauzimu:

Kukhala Mwa Khristu

Poyamba, tingathe kupeza thandizo la Khristu mu kuumba khalidwe la umulungu pakukhala, kapena kukhalabe mwa Iye. Tingathe kukhala ngati Khristu ngati tikhala mwa Iye basi. Yesu adati, "Monga nthambi siingathe kubala chipatso payokha, ngati siikhala mwa mpesa; motero mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine" (Yoh. 15:4). Kukhalabe mwa Yesu ndiko kupeza moyo kuchokera kwa iye pakupitirizabe kukhala mu mau ndi kupezeka kwake. Timachita pokhala apemphero lodzipereka, kusanthula mau pafupipafupi, ndi kumudalira iye kwathunthu kuti akwaniritsa zosowa zathu zonse.

Kusendeza Chifupi ndi Mulungu

Timakhazikitsanso khalidwe la Khristu pakusendezabe chifupi naye tsiku ndi tsiku. Yakobo akutitsimikizira, "Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu" (Yak. 4:8). Monga m'mene ziliri ndi kukhala mwa Yesu, timasendeza kwa Mulungu kudutsira mu pemphero, kulambira, ndi kutumikira mokhulupirika. Pamene tisendeza chifupi ndi Khristu, timasinthika pokhala ofanana naye. Paulo adalemba, "Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyerera monga mwa kalirole ulemelero wa Ambuye, tisandulika m'chithunzithunzi chomwechi kuchokera kuulemelero kunka kuulemelero, monga ngati kuchokera kwa Ambuye Mzimu" (2 Ako. 3:18).

Kuyenda Mwa Mzimu

Pomaliza, timakhazikitsa khalidwe la Khristu poyenda mwa Mzimu. Kuyenda mwa Mzimu ndi kukhala moyo womvera Mzimu Woyera. Ndiko kumvera malamulo ake. Paulo adati "timayeretsedwa ndi Mzimu Woyera" (Arom. 15:16). Izi zitanthauza kuti Mzimu wa Mulungu amatipatsa ife mphamvu yomwe timafuna kuti tikhale ngati Yesu. Paulo adalimbikitsa Akhristu aku Galatiya, "Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako za thupi" (Agal. 5:16).

Solomoni adalemba kuti, "Nzeru ipambana, tatenga nzeru; m'kutenga kwako konseko utenge luntha. Uilemekeze, ndipo idzakukweza; idzakutengera ulemu pamene uifungatira" Miy. 4:7-8). Zomwezinso zingathe kunenedwa kwa mbusa wa Chipentekoste. Ngakhale ikutengera zonse uli nazo, tengani khalidwe; lilemekezeni, ndipo lidzakukwezani; ifungatireni, idzakubweretserani ulemu. Pamwamba pa zonse, mbusa wa Chipentekoste akuyenera kukhala munthu wakhalidwe.

~ Mutu 4 ~

Munthu AmeneWakonzekera Bwino

Monga zimakhalira ndi bungwe lina lililonse, mpingo uzitsogoleredwa ndi iwo amene akonzeka bwino pa ntchitoyo. Mlaliki wodziwika bwino padziko lapansi nthawi ina adati, “Ndikadadziwa kuti ndili ndi zaka zitatu zolalikila uthenga wabwino, ndikadakhala ndi zaka ziwiri zoyambirira kuti ndikonzekere.” Mbusa wina wopambana adaonetsetsa mwanzeru, “Chipambano chimachitika pamene mwayi wakumana ndi kukonzekera.” Anthu onsewa ankatsindika za kufunika kwa kukonzekera mu utumiki wauthenga wabwino.

Paulo adamulembera Timoteo amene adamusankha kukhala mbusa woyang’anira mpingo wa ku Aefeso, “Ngati munthu akhumba udindo wa woyang’anira (mbusa), aifuna ntchito yabwino” (1 Tim. 3:1). Kenako Paulo adatchulaposo zoyenereza munthu kutumikira mu ntchito ya ubusa. Chimodzi mwa zoyenereza zimenezi chidali, “Asakhale wophunza” (v. 6).

Mau a chilankhulo cha chihelene (Giriki) omwe amasuliridwa kuti “wophunza” munkhaniyi ndi *neophytos*, amene atanthauza kuti “wongodzalidwa kumene” kapena “munthu woyamba kumene.” Izi ndi zosiyana ndi kulongosola kwina komwe Paulo akugwiritsa ntchito kwa mbusa, komwe ndi, “mkulu wampingo,” kapena *prebyteros* muchihelene. Mau awa amalankhula zomwe munthu wadutsamo ndi kukhazikika, ndipo ziyimilira chikonzekero (1 Tim. 5:17-19; Tit. 1:5). Paulo akuti mbusa asakhale woyamba kumene mukuyenda kwake

ndi Khristu. Mosiyana ndi izi, iye akuyenera kukhala munthu wokhazikika bwino mu chikhulupiriro ndi okonzeka bwino ku ntchito ya utumiki.

Mlaliki wachichepere wa Chipentekoste nthawi inaadauzapo mphunzitsi wamkulu pa sukulu ya Baibulo,"Sindisowekera maphunziro; chokhacho ndifuna ndiko kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu monga okhulupirira pa Tsiku la Pentekoste." Ngakhale kuti izi zidachitika chomwechi, mauwa ndi opusa. Chomwe mlaliki wachichepereyu sadazindikire ndichakuti lisadafike Tsiku la Pentekoste, ophunzira khumi ndi awiriwo adatenga zaka zitatu akuphunzira pansi pa Yesu. Ngakhale kuti mlaliki wachichepereyu adakhonza zakufunika kwa kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera, iye adalakwitsa zokhudza kaonedwe kake ka kufunika kwa kukonzekera kwa utumiki kwa uzimu, nzeru, ndi zochitika zenizenizo.

Yesu adasankha ophunzira ake khumi ndi awiri "kuti akhale ndi Iye, ndi kuti akawatume kulalikira" (Marko 3:14). Iye asadawatume kuti apite kudziko lonse kukalalikira uthenga wabwino, Iye adali ndi ma ola osawerengeka ndi iwo kuwakonzekeretsa ku ntchitoyi.

Mutu uno ukulongosola za kufunikira kwa mbusa wa Chipentekoste kuti akhale wokonzeka. Ukubweretsa poyera madera ena omwe chikonzekero chimafunikira. Kenako ukulankhula za momwe mbusa wa Chipentekoste angapezere ndi kusungabe chikonzekero chofunikiracho.

MADERA A CHIKONZEKERO

Kukonzekera kwa ubusa kumamulora yemwe akukhumba utumiki kuti akhazikitse maluso ofunikira ndi maonedwe ofunikira pokwaniritsa mayitanidwe. Zikhoza kuganiziridwanso kuti ndizipangizo kapena zida za mbusa zoti akhalirebe ndi moyo. Kukonzekera kokwanira bwino sikuti kudzango kuyenerezani kuti mugwire ntchito yanu mwaubwino ayi, kudzakutetezani ku kulephera munthawi zakulemedwa mumtima kapena chiopsezo. Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kukhala wokonzekera bwino munjira zosachepera zisanu:

Kukonzekera Mwa Uzimu

Pamwamba pa china chilichonse, mukuyenera kukhala okonzekera mwa uzimu za ntchito yanu monga mbusa wa Chipentekoste. Zingatheke bwanji kuti muwauze ena za chisomo cha Mulungu ngati inuyo eni simudakumane nacho chisomocho? Choncho, kukhala mbusa weniweni wa Chipentekoste kumafunikira

kubadwa mwatsopano kwenikweni (Yoh.3:3-7) ndi kukhala odzadzidwa moonadi ndi Mzimu Woyera (Mach. 1:8; Aef. 5:18). Kuonjezera apo, mukuyenera kumakhala moyo wolemekeza Yesu mokhulupirika (1 Yoh. 2:6), komanso wodzipereka kotheratu kwa Khristu ndi utumwi wake (Mat. 16:24).

Paulo adamukumbutsa Timoteo kuti "pakuti chizolowezi cha thupi chipindula pang'ono, koma chipembedzo chipindula zonse" (1 Tim. 4:8). Paulo adagwiritsa ntchito chining'a cha maphunziro ichi pofuna kuonetsera mwambo wauzimu omwe umafunika pokonzekera utumiki waubusa (onaniso 1 Ako. 9:24-27). Iye ankamuuza Timoteo kuti monga momwe munthu wochita mpikisano wothamanga ayenera kudzikonzekeretsa bwino, nayeso mbusa ayenera kudzikonzekeretsa bwino mwauzimu ku ntchito yautumiki. Osewera mpira yemwe akana kuchita zokonzekera adzadzichotsa yekha mu gulu lake. Chomwechonso, mbusa yemwe amakana kugwiritsa ntchito mwambo wauzimu adzadzichotsa yekha mu utumiki.

Kukonzekera Mwa Baibulo

Chachiwiri, mukuyenera kukonzekera mwa Baibulo kuti mukhale mbusa wa Chipentekoste wamachitachita. Izi zikutanthauza kuti mukhale ndi chidziwitso chokwanira cha malembo. Ntchito yayikulu ya mbusa aliyense ndiko kudyetsa nkhosa za Mulungu powaphunzitsa mau a Mulungu mokhulupirika. Kuphunzitsa bwino mau a Mulungu kudzachititsa oyera mtima kuti akule mwa Khristu (1 Pet. 2:2), kuwakonzekeretsa kuti asatengeke ndi aphunzitsi achinyengo (Mach. 20:28-29), ndi kuwapatsa zida zochitira utumiki wachikhristu (Aef. 4:11-12). Ndi zodabwitsa kuti Paulo kawiri konse adamuuza Timoteo kuti mbusa ayenera kukhala ndi "kuthekera kophunzitsa" (1 Tim. 3:2; 2 Tim 2:24). Utumiki wamphamvu wophunzitsa ukhoza kumangidwa pa maziko a chidziwitso chachikulu cha Baibulo basi. Pofuna kuphunzitsa bwino anthu a Mulungu, mwayenera kudziwa momwe mungamasulire molondola ndi kugwiritsa ntchito "mau a choonadi" (2 Tim. 2:15).

Kukonzekera Mwa Chikhalidwe

Chotsatira, pakufunika mukhale okonzekera utumiki mu chikhalidwe monga mbusa wa Chipentekoste. Mwayenera kumakhala moyo wolemekeza Yesu ndi wachiyero. Paulo adalemba kuti woyang'anira kapena mbusa "ayenera kukhala wopanda chilema…. wosati wachiwawa, wopanda ndeu, wosati wachisiriro chonyasa" (Tit. 1:7). Iye adaonjezeranso kuti mbusa akhale "wolungama, woyera mtima, wodziletsa" (v. 8). Momwemonso, iye adamuuza Timoteo kuti

woyang'anira ayenera kukhala "wopanda chilema, mwamuna wa mkazi m'modzi…wosakhumba chuma" (1 Tim. 3:2). Aliyense amene sachita bwino m'madera awa amoyo wadzichotsa yekha mu utumiki. Munthuyo ayenera kuusiya utumiki kufikira atayamba kuchita bwino m'makhalidwe awa.

Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kusamalitsa machimo atatu aakulu amene akola ndi kuchotsa atsogoleri ochuluka achipembedzo. Makhalidwe aakulu atatu amenewa ndi dyera (chikondi chapandalama), chisiliro (kukhumba kosayenera), ndi zokhumba za dziko (kufuna kusiliridwa ndi ena komanso kufuna kukhala ndi ulamuliro pa ena). Palibe mulingo uliwonse wa mphatso kapena kudzodza komwe kungalimbe pakulephera kusamalitsa madera amenewa.

Mu kalata ya Paulo yopita kwa okhulupirira aku Galatiya, iye adawachenjeza zokhudza kudziphathika ku zokhumba za chibadwidwe chauchimo (Aga. 5:19-21). Koma, iwo ayenera kukhala ndi chipatso cha Mzimu (vv. 22-23). Kenako, Paulo adawaonetsera iwo njira yakudzuka kuchoka ku kukhala ndi khalidwe loipa kupita ku khalidwe labwino: "Koma iwo a Khristu Yesu adapachika thupi, ndi zokhumba zake, ndi zilakolako zake. Ngati tili ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende" (vv.24-25). Mtumwiyu adapitilizanso kuwauza Agalatiya kuti "Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako cha thupi" (v. 16).

Kukonzeka Mu Nzeru ndi Maganizo

Pomaliza, mukuyenera kukonzekera mu nzeru ndi m'maganizo ngati mufuna kuti muyigwire ntchito ya utumiki mochitachita. Mukunena kwina, pakufunika kuti muziganiza bwino, komanso muzikwanitsa kulamulira maimvaimva anu ndi kuchitapo kanthu moyenerera pa zokhoma zomwe mukumana nazo.

Paulo adamulembera Tito, "Pakuti woyang'anira ayenera kukhala wopanda chilema, ngati mdindo wa Mulungu; wosati waliuma, wosapsa mtima msanga…wopanda ndeu,…komatu wokonda…wodziweruza… wodziletsa" (Tit. 1:7-8). Mu kalata yake yoyamba yopita kwa Timoteo, mtumwiyu adaonjeza kuti, "Ndipo kuyenera woyang'anira akhale…wodzisunga, wodziletsa…wosati woledzera kapena womenyana ndeu; komatu wofatsa, wopanda ndeu" (1 Tim. 3:2). Onetsetsani momwe khalidwe lililonse losankhidwa m'mwambamu likulankhulira za kukhwima mu nzeru komanso maganizo. Monga mbusa wa Chipentekoste, yesetsani kukhala nao makhalidwe amenewa mmoyo ndi utumiki wanu.

Mbusa yemwe ndi woyima bwino mu nzeru ndi wokhwima m'maganizo adzakhala ndi kudzidalira pogwiritsa ntchito mphatso zopatsidwa ndi Mulungu ndi kuthekera kosiyanasiyana. Kulimbika mtima uku kudzawathandizira iwo pakuthana ndi nyengo zolimba ndi kuchita ziganizo zofunikira kwambiri. Kudzawatetezanso kuti asathawe maudindo awo wovuta monga kulengeza nkhani zoipa, kuteteza mpingo kwa aphunzitsi achinyengo, ndi ntchito zina zovuta.

NJIRA ZA KAKONZEKEREDWE

Podziwa phindu la kakonzekeredwe kabwino, mbusa wa Chipentekoste wanzeru adzayesetsa mwanjira iliyonse kuti adzikonzekeretse yekha ku utumiki. Tiyeni tione njira zitatu zokwaniritsira izi:

Kudutsira mu Zodutsamo M'moyo

Poyamba, mungathe kudzikonzekeretsera utumiki wanu pofunafuna zinthu zokumana nazo. Njira zitatu zofunikira zopezera ukadaulo umenewu nazi:

1. Kugwira ntchito mumpingo wa pamalo. Msonkhano wa pa malo ndi malo achikhalire oyambirapo utumiki wanu. Paulo ndi Barnabasi ankachita utumiki mu mpingo waku Antiokeya pamene Mzimu Woyera adawatsogolera ku utumiki wautumwi (Mach. 11:25-26; 13:1-3). Paulo adapitiliza kutenga anthu ena othandizana naye ntchito yautumwi pakati pa iwo amachitachita m'mipingo ya pamalo. Mwachitsanzo, adatenga Timoteo kuchokera ku mpingo waku Listara (16:1-2), Sopatere kuchokera ku Bereya, Aristariko ndi Sekundo kuchokera ku Atesalonika, ndi Gayo kuchokera ku Derbe (20:4). Anthu awa adaphunzira momwe angatumikilire m'mipingo yawo ya pamalo. Chifukwa chakatumikiridwe kawo, iwo adayenerezedwa kukachita utumiki waukulu.

Chifukwa cha ichi, mufunefune mwayi wotumikira mu mpingo wanu wa pamalo monga mbusa wa Chipentekoste. Mukhale okonzeka kudzipereka pamene mwayi otumikira wapezeka. Potengapo mbali pa mautumiki apa mpingo wa pamalo, mudzapeza ukadaulo wamtengo wapatali, mphatso zanu zauzimu zidzalimbikitsidwa, ndipo maitanidwe anu autumiki waukulu adzatsimikizika.

2. Kutumikira pansi pa mbusa wakale muutumiki. Njira inanso yamphamvu yokonzekerera utumiki wa Chipentekoste ndi maphunziro akusulidwa. Maphunziro akusulidwa amachitika pamene mlaliki woyamba kumene ayenda pamodzi ndi mbusa amene ndi mkhalakale mu utumiki ndipo amaphunzira kuchokera kwa iye. Umu ndi momwe Yesu adaphunzitsira ophunzira ake (Marko.

3:14-15). Iye adawauza kuti, "Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu" (Marko. 1:17). Pamene iwo adayenda ndi kutumikira ndi Yesu, adaphunzira kutumikira pamene Iye ankatumikira. Iye adati, "koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wake" (Lk. 6:40).

Zitsanzo zina za m'Baibulo za kusulidwa ndi Mose ndi Yoswa (Ekso. 24:12-13), Eli ndi Samuele (1 Samu. 2:11), Eliya ndi Elisa (1 Mafu. 19:19-21), ndi Paulo ndi omuthandizira utumwi— kuphatikizapo Timoteo, Tito, ndi ena. Kutumikira pansi pa mbusa yemwe ndi mkhalakale kudzakuchititsani kuti muzindikire zamoyo wampingo komanso kuphunzira ntchito ya ubusa.

3. Kugwira ntchito ndi ena. Mungathenso kupeza ukadaulo wamtengo wapatali pogwira ntchito ndi ena mu magulu autumiki. Magulu awa angathe kukhala a zopembedzera, azautumwi, odzala mipingo, ndi ena. Phindu limodzi logwira ntchito ndi ena mmagulu ndilakuti zidzakuthandizani kuti muphunzire momwe mungagwilire ntchito mwa umodzi ndi antchito anzanu mu utumiki.

Kudzera mu Kuphunzira Koma Mosalowa M'kalasi

Njira ina yomwe mungadzikonzekeretsere nokha ku utumiki ndi kudzera mu "kuphunzira kosalowera m'kalasi." Kuphunzira uku ndikomwe kumachitika kudzera mu njira zina kupatulako kulowa m'kalasi ndikumaphunzira. Ngakhale kuphunzira uku kulimoteromo, kusayesedwe kuti nkopanda tanthauzo kapena koononga ayi. Kukhonza kukhala mwadaladala koma kwa mphamvu. Maphunziro awa ndi monga kusanthula Baibulo pawekha, kuwerenga mabuku ndi nkhani zina, kuchita nawo misonkhano, ndi kuphunzira kudzera mu nthambi ya sukulu ya baulo. Iz zikulongosoledwa motere:

1. Kusanthula Baibulo panokha. Njira imodzi yamtengo wapatali ya kuphunzira kosalowera m'kalasi ndi kuwerenga ndi kusanthula Baibulo panokha. Kuwerenga Baibulo mu chaka chonse ndi machitidwe oyenerera. Zikhoza kuthandiza kuti mukhale olumikizika ndi m'mene malembo akuyendera. Njira ina yamtengo wapatali yowerengera Baibulo ndiko kuwerenga mwachibwereza buku losankhika la m'Baibulo. Wophunzira wina wa Baibulo adati, "Chinsinsi cha kulidziwa Baibulo si kuliwerenga koma kuliwerenganso." Mukamaliwerenga buku losankhidwa kangapo, mudzazindikira mavumbulutso ambiri mu zoonadi zochuluka zophunzitsidwamo.

Kuseri kwa kungowerenga chabe Baibulo, mudzafuna kukhazikitsa kusanthula Baibulo mwandondomeko yapamwamba. Ngati ndi kotheka, pezani

Baibulo loti muzigwiritsa ntchito lokhala ndi akalozera (Mapu), ndondomeko ya buku ndi kayambidwe, kutambasulira ndime, nkhani, ndi zithunzi. [1]

2. Kuwerenga mabuku ndi nkhani. Njira yina yamtengo wapatali ya maphunziro osalowera m'kalasi kwa mbusa aliyense wa Chipentekoste ndiko kuwerenga mabuku osankhika ndi nkhani zina koma molingalira bwino. Wina wake adazindikira molondola, "Atsogoleri ndi awerengi." Choncho, mufunikira kuti mukhale a njala yowerenga. Kuwerenga kwa tsiku ndi tsiku kudzakuthandizani kunola ubongo wanu, kukuza maganizo anu ndi kupititsa patsogolo maluso akaganizidwe kanu. Kudzakupatsaninso mavumbulutso atsopano okhudza mavuto amoyo ndi utumiki. Kuwonjezera apo, chikhalidwe chakuwerenga chidzakuthandizani kuwonjezera chidziwitso chanu cha mau, potero kuonjezera kuthekera kwa kalankhulidwe kanu.

Komabe, mukuyenera kukhala osamalitsa pakasankhidwe ka zowerenga zanu. Mabuku ambiri ndi nkhani zambiri zopezeka ku Afirika lero zimalimbikitsa machitidwe ndi makhalidwe otsutsana ndi malembo (onani 1 Tim. 4:7; 2 Yoh. 1:7-8). Pewani zowerenga zamtundu umenewu.

3. Kukhala nawo pa misonkhano ndi maphunziro ena apadera. Mukhozanso kukhazikitsa maluso anu autumiki pokhala nawo pa misonkhano ya abusa ndi maphunziro ena. Misonkhano iyi kawirikawiri imakonzedwa kuti ithandize abusa kuti apititse patsogolo maluso awo autumiki. Misonkhanoyi imatakasanso abusa ofooketsedwa ndi kuwathandiza kuti apeze mavumbulutso atsopano a m'malembo ndi ntchito ya pampingo. Maphunziro apadera amazindikiritsa abusa za machitidwe a mipingo, ndipo amathandiza kukhazikitsa maimvaimva ogwilira ntchito pamodzi pakati pa ogwira nawo ntchito mu utumiki.

Kudutsira M'maphunziro a M'kalasi

Pomaliza, pezani maphunzirowa monga mbusa wa Chipentekoste ngati kuli kotheka. Maphunziro awa ndi omwe amachitidwa ndi sukulu zopezeka pamalo ndi zina zosapezekapamalo. Umwayi wa maphunziro oterewa umaphatikizapo zotsatirazi:

---

[1] Baibulo lachipentekoste, labwino kwambiri kulisanthula ndi *Baibulo la Moyo Wochuluka*, lomwe limadziwikanso kuti *Baibulo la Moyo Mwa Mzimu*, kapena "Baibulo la Moto." Baibulo ili latanthauziridwa muzilankhulo zambiri.

1. Maphunziro asukulu osati za chipembedzo. Pulaimale, sekondale, ndi sukulu zaukachenjede ndizofunikira kwa mbusa wa Chipentekoste ku Afirika. Sukulu izi zimathandiza kukonzekeretsa ophunzira zokhudza moyo mudziko lamakonoli. Kudzera m'menemo, ophunzira amaphunzira kawerengedwe, kalembedwe, ndi kupeza mayankho a masamu. Kumeneko amaphunzira mbiri, maphunziro okhudza malo, ndi maphunziro ena ofunikira. Kwa yemwe akufuna kukhala mbusa wa Chipentekoste, kufunikira kwa maphunziro a sukuluzi nkwakukulu. Amathandiza kudzutsa chidwi chao, kukulitsa kaganizidwe kawo, ndi kuwadziwitsa za zomwe zikuchitika mdera.

2. Sukulu za Baibulo. Ndizofunikiranso kwambiri kuti mukachite maphunziro ku sukulu zodziwika bwino ngati mkotheka kutero. Munthu yemwe akufuna ntchito ya udotolo wachipatala angakhale wopusa motani atamakana maphunziro omuyenereza zachipatala! Momwemonso iye amene amadzitcha yekha mbusa wa Chipentekoste akhoza kukhala wopusa pamene anyalapsa maphunziro a zautumiki. Mipingo yambiri m'maiko imafuna kuti abusa awo akaphunzire ku sukulu za Baibulo. Kaya ndi kofunika kwa mpingo kukhala ndi maphunziro otere kapena ayi, mbusa wanzeru wa Chipentekoste adzafunafunabe maphunziro otere.

3. Maphunziro a Baibulo ena asukulu ya nthambi. Sukulu zina za Baibulo zimapereka maphunziro otere ndi maphunziro ena omwe munthu amachita payekha. Maphunziro awa angathe kuperekedwa pochita pawekha, pa mauthenga a palamya, kapena pa luso la makono la intaneti. Izi zimalora kuti mbusa aziphunzira ali kunyumba kuchita utumiki. Ndi njira yapamwamba kwambiri kwa mbusa kuti apititse patsogolo chidziwitso chake ndi maluso ake.

Pakadali pano, mipingo ya Assemblies of God mu Afirika yonse ili ndi sukulu za maphunziro autumiki zopitilira mazana atatu (300). Sukulu izi zimapereka maphunziro kwa ophunzira omwe ndi a Assemblies ndi mipingo ina. Mbusa wa pamalo wa Assemblies of God mdera lanu angathe kukuthandizani kuti mupeze sukulu m'dziko lanu.

4. Maphunziro ena oonjezera aukachenjede. Atumiki ena aChipentekoste mu Afirika amafuna kuti apitilize maphunziroapamwamba kapena ena apadera. Izi ndi zoona ndithu makamaka kwa aphunzitsi a sukulu za ukachenjede za Baibulo ndi maseminare. Ndizofunikira kwambiri kuti munthu akapitirize maphunziro ake ku sukulu yovomerezeka ya Chipentekoste. Mipingo yambiri ya Assemblies of God mu Afirika imapereka maphunziro a digiri ya Ukadaulo (*Masters*). Maphunziro a digiri yapamwamba amaperekedwa ndi sukulu ya utumiki ya Pan-Africa

(PAThS). PAThS ndi sukulu yovomerezeka bwino, yoyendetsedwa ndi mpingo wa Assemblies of God ku Lome, Togo, ndi madera ena a mayiko amu Afirika omwe ndi nthambi zake. Maphunzirowa amaperekedwa mu chingerezi ndi mu chifalansa.

KUKONZEKERA KOPITILIRABE

Choonadi ndi chakuti kukonzekera kwanu, monga mbusa wa chipentekoste, sikufika kumapeto. Mukuyenera kukhala ophunzirabe moyo wanu onse. Moyo wanu uzidziwika ndi kufunitsitsa kwanu kopita patsogolo. Paulo adatsimikizira za izi pomwe adalemba kuti, "Sikunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndatha kukonzeka wamphumphu; koma ndilondetsa, ngatinso ndikachigwire ichi chimene anandigwirira Yesu Khristu" (Afil. 3:12).

Kukhumba uku kopitabe patsogolo m'moyo kuyenera kukhale kopitilira m'moyo mwanu. Mupitilizebe kudzikonzekeretsa nokha *mwauzimu* pofunafuna kukhalabe ndi chidzalo cha Mzimu Woyera komanso kuchita miyambo ya uzimu ya pemphero, kusala, kulambira, ndi kulingalira malembo.[2] Mudzipitirizabe kudzikonzekeretsa nokha *m'malembo* kudutsira mukusanthula malembo mwa mwambo, ndi kufuna kupitiriza maphunziro ngati Mzimu angatsogolere choncho.[3]

Kuonjezera apo, mufunefune kudzipititsa nokha patsogolo mu *chikhalidwe*. Mu mau a Solomo, mukuyenera kutchinjiriza mtima wanu ku choipa, kusamalitsa kwambiri njira ya mapazi anu (Miy. 4:23-27). [4]

Pomaliza, mukuyenera kupitiliza kudzikonzekeretsa nokha mu nzeru ndi maganizo monga mbusa wa Chipentekoste. Mukhonza kuchita izi kudutsira mukuwerenga ndi kusanthula mwa mwambo, ndi kumulora Mzimu ndi Mau a Mulungu kuti agwire ntchito mwa mphamvu m'moyo wanu, kukuumbani kuti mukhale nawomaonekedwe Akhristu (2 Ako. 3:18).

---

[2] Kuti mudziwe zambiri za kukonzekera kwa uzimu, onani Mutu 15; "Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu."

[3] Kuti mudziwe zambiri za ubale wa mbusa wa Chipentekoste ndi Baibulo, onani Mutu 9: "Amakhulupirira Baibulo.

[4] Kuti mudziwe zambiri za kukonzekera kwa chikhalidwe, onani Mutu 3: "Munthu wa Khalidwe Labwino."

~ Gawo 2 ~

ZINTHU ZOFUNIKIRA ZOYAMBIRIRA ZA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

~ Mutu 5 ~

Zofunikira Zoyambirira Za Utumiki

Mbusa wina mkhalakale anali pazokambirana ndi gulu la ophunzira Baibulo achidwi kwambiri. Ophunzira wina adamfunsa, “Aphunzitsi, Kodi munakwanitsa bwanji kumanga Mpingo waukulu motere? Kodi ndi chiyani chomwe mungaloze kuti chakuthandizirani kupambana mu utumiki?” Yankho lake linadabwitsa ophunzirayo. Iye anati, “Kuti uchite bwino kwambiri ukuyenera kusiya chongokhala chabwino.” Poona kudabwitsika pa nkhope pa ophunzirayo, adafotokozera, “M’moyo pali zambiri zabwino zomwe mungathe kuzichita. Dziko lapansi lidzaika zofuna zake zochuluka pa inu. Ma membala ndi akulu ampingo adzakhala ndizoyembekezera kwa inu. Abusa ena adzachita zinthu zina ndipo adzayembekeza inuyo kuchita chimodzimodzi.”

Mbusa wakaleyu anapitiriza, “Zinthu zonsezi zikhoza kukhala zabwino. Koma pokhala munthu wa Mulungu mwamuna kapena mkazi, mukufunikira kumfunsa Iye, ‘Ambuye, kodi mukufuna kuti ine ndichite chiyani?’ Kenako, ukamva liwu la Mulungu, uchite zimene Iye akunena. Zinthu zina zikhoza kukhala zabwino, komatu zimene Mulungu akukuuza kuti muchite ndiye zabwino kwambiri. Mulungu adzabweretsa anthu mumpingo wanuwo kukathandizira kuchita zinthu zinazo. Inuyo mukuyenera kuchita molunjika pachimene Mulungu wakuuzani kuti muchite.”

Mbusa wakaleyu amayankhula za kukhazikitsa zofunikira za utumiki. Ndibwino kuti zinthu zofunikira kuti zichitike koyambirira zitero. Zinthu

zofunikira zoyambirira ndizomwe umazichita usanayambe kuchita zofunikira pang'ono.

ZOFUNIKIRA ZA BAIBULO

Yesu ndi ophunzira ake anali paulendo kuchokera ku Yudeya kupita ku Galileya. Ataima panjira anawauza iwo, "Ndipo anayenera kupita pakati pa Samariya" (Yohane 4:4). Ichi chinadabwitsa ophunzirawo chifukwa simmene amayenera kuchitira. Atafika ku mzinda wotchedwa Sikari anamvetsetsa chifukwa chake Yesu anayenera kudzera ku Samariya. Kunali anthu ambiri otaika amene anali okonzeka kulandira uthenga wachipulumutso. Yesu amafuna kuwaphunzitsa ophunzira ake kukolora kholora.

Panthawi inanso Yesu anauza ophunzira ake, "Ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga" (Mateyu 16:18). Kenaka anawalamulira iwo, "Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera" (Mateyu 28:19). Munthawi zonsezi Yesu amayankhula za zoyambirira zimene adazikhazikitsa za iye komanso ophunzira.

Potsatira chitsanzo cha Mbuye wawo, atumwi nawo adakhazikitsa zofunikira za utumiki. Zofunikira zoyambirirazi kunali kuchita ntchito imene Khristu anawapatsa. Tsiku lina gulu lina laanthu amu mpingo linadza kwa atumwi ndi dandaulo. Akazi ena amasiye samawerengedwa pogawa chakudya, ndipo amafuna kuti atumwi awathandize pabvuto lawo. Panthawiyi atumwi anali atakhazikitsa kale zofunikira mu utumiki ndipo anawayankha iwo, "Sikuyenera ife kuti tisiye kulalikira mau a Mulungu ndi kutumikira podyerapo" (Mach. 6:2).

Kusamalira azimai amasiye omwe samawerengedwa pachakudya kunali kwabwino ndikofunikira, koma sichimene Khristu anawalamulira atumwi kukachita. Ndipo iwo m'malo mwake anapempha mpingo kuti usankhe othandizira kuti athane ndichosowekerachi pamene iwo anapitiliza ndichofunikira choyambirira chakupemphera ndi kulalikira. Chotsatira chake, "Ndipo mau a Mulungu anakula; ndipo chiwerengero cha ophunzira chidachulukatu ku Yerusalemu; ndipo khamu lalikulu la ansembe linamvera chikhulupirirocho (v. 7).

Mutu uwu ufotokoza zaubwino wake wa zofunikira za utumiki kwa Mbusa wa ku Afirika lero lino.

KUZINDIKIRA ZOFUNIKIRA ZOYAMBIRIRA ZAUTUMIKI

Kodi ndizofunikira zake ziti zimene Mbusa wa Chipentekoste ayenera kukhala nazo? Pamene pali zambiri zabwino zimene akhoza kuzichita, pali zochepa chabe zimene ayenera kuzichita. Zinthu zisanu ndi ziwiri za zofunikirazi ndi monga (1) kutumikira cholinga cha Mulungu, (2) kukwaniritsa maitanidwe a Mulungu, (3) kufikira otaikawo, (4) kulalikira mau a Mulungu, (5) kupemphera, (6) kugwiriziza zikhulupiliro za PENTEKOSTE, ndi (7) kukonzekeretsa anthu a Mulungu ku ntchito ya utumiki. Tiyeni tsono tione mfundo iliyonse payokhapayokha za zofunikira za utumiki:

Kutumikira Cholinga cha Mulungu

Poyambirira, mbusa wa Chipentekoste ayenera kuika kutumikira cholinga cha Mulungu kukhala chofunikira kwambiri. Atatha kuyesedwa kwake m'chipululu, Yesu anabwerera ku Galileya.Alikumeneko, analowa msunagoge ku Nazarete nayamba kuwerenga m'buku la Yesaya: "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyanso, kutulutsa ndi ufulu ophwanyika, kulalikira chaka chosankhika cha Ambuye" (Luka 4:18-19). Yesu amadziwazofunikira za Atate ake pa moyo wake ndi utumiki. Iye anazindikira kuti Atate anamtuma Iye kukatumikira cholinga cha Atatewo. Mulungu Atate anamtumanso Mwanayo ku chiombolo cha anthu onse (Mateyu 20:28).

Monganso Yesu, chomwecho Mbusa wa Chipentekoste ayenera kudzipereka yekha kutumikira cholinga cha Mulungu. Yesu anauza ophunzira ake, "Monga Atate wandituma Ine, Inenso ndituma inu" (Yohane 20:21). Monganso Mulungu anatuma Yesu ku dziko lino lapansi kukatumikira cholinga Chake, Yesu tsopano akutumanso inu mdziko lapansi kukachita chimodzimodzi. Cholinga cha Mulunguchi nthawi zina chimatchedwa kuti *missio Dei*, komwe ndikuombola ndi kuitanira kwa Iye mwini anthu a mtundu uliwonse, chinenero chilichonse komanso fuko lililonse la pa dziko lapansi (Chivu. 5:9).[1]

[1] Kupeza zochuluka za ntchito ya Mbusa pokwaniritsa cholinga cha Mulungu, onani Mutu 31: "Utsogoleri wa Utumwi" ndi Mutu 40: "Kukhazikitsa Dongosolo la Utumwi la Mpingo Wapamalo."

Kukwaniritsa Maitanidwe a Mulungu

Chachiwiri, mbusa wa PENTEKOSTE ayenera kuika ngati chofunikira patsogolo kukwaniritsa maitanidwe a Mulungu pamoyo wake. Yesu sanatayeko chindunji cha chokwaniritsa maitanidwe a Mulungu pamoyo wake. Munthawi yake ya mdima anapemphera kwa Atate wake, "Koma si kufuna kwanga ai, komatu kwanu kuchitike" (Luka 22:42). Momwemonso, Mbusa wa Chipentekoste mu Afirika ayenera kumvetsetsa maitanidwe a Mulungu pamoyo wake ndikuyesetsa kukwaniritsa maitanidwewo. Mulungu anaikiratu njira ya otumikira aliyense yomwe ayenera kuyendamo. Mbusa aliyense wa Chipentekoste akuyenera kuipeza njirayi. Ndipo akuyenera kuyendamo kufikira atamaliza ntchito yake (Ahebri. 12:1-2; 2 Timoteo. 4:7).

Kufikira Otaikawo

Chachitatu, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuika poyambirira kufikira otaikawo. Ichinso chinali choyambirira cha Yesu. Amachitira umboni, "Pajatu Mwana wa Munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho (Luka 19:10). Kufikira otayikawo chikuyenera kukhala choyambirira cha wina aliyense wakufunafuna kutsatira Khristu. Yesu analamulira, "Mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse" (Marko 16:15).

Lamulo limeneli la Khristu lidzakhalabe kufikira Iye atabweranso kuchokera kumwamba (Mateyu 24:14). Monga Mbusa okhulupirika wa Chipentekoste uyenera kutsogolera kuupangitsa mpingo kukhala odzala ndi mphamvu zakulalikira ndi utumwi. Mbusa akhoza kuchita zimenezi mu njira ziwiri:

Njira yoyamba ndiyoti akuyenera kukhala chitsanzo ku mpingo potenga nawo gawo kugawana za uthenga wabwino ndi ena, kufunafuna kuwatsogolera kwa Ambuye. Pamene mamembala akuona inu mukuchitira umboni amakhala olimbikitsika kukachitiranso umboni. Yachiwiri, Mbusa akuyenera kuonetsera kukhuzika kwake kwa otaikawo popereka mowolowa manja ku ntchito ya utumwi, komanso popemphelera mokhudzika mitundu yomwe sinafikiridwe ya mu Afirika ndi madera ena. Mbusayu akuyenera kuukonzekeretsa ndikuulimbikitsa mpingo kuti uchite momwemo. Akuyeneranso kuwonetsetsa kuti usodzi wa anthu ndi

utumwi ukukhala pamwamba pazofunikira mumadongosolo ampingo ndi kagwiritsidwe ntchito ka ndalama.[2]

Kulalikira Mau

Chachinayi, mbusa wa PENTEKOSTE akuyenera kuika kulalikira kwa mau a Mulungu kukhala chofunikira. Paulo anamuyamikira Timoteo mwana wake m'chikhulupiriro, "Lalikira mau; chita panthawi yake, popanda nthawi yake; tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitso" (2 Timoteo 4:2). Kulalikira Mau kumakhudzana ndikulengeza uthenga wabwino kwa otaikawo, kulangiza ndi kulimbikitsa okhulupirika mnjira ya Ambuye. Yesu analamulira, "Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse" (Marko 16:15). Anawalamuliranso, "Dyetsa nkhosa zanga" (Yohane 21:17). Kuti uthe kulalikira bwino, ukuyenera kudzipereka pakagwiritsidwe ntchito koyenera ka mau a choonadi (2 Timoteo. 2:15). Kuti uchite zimenezi, ukhale ophunzira wa chidwi pa mau a Mulungu.[3]

Kupemphera

Chachisanu, mbusa wa Chipentekoste ayenera kuika pemphero koyambirira. Pokhala moyo odzipereka wapemphero, umaonetsera kudalira kwako paMulungu. Ndipo kuposera apo ndiye kuti ukutsatira mapazi a Yesu ndi atumwi. Baibulo limanena za Yesu kuti munthawi yake ya pansi pano, "adapemphera mapemphero ndi kulira ndi misozi" (Ahebri. 5:7; fanizilani Marko 1:35; Luka 5:16). Limanenanso za atumwi kuti anali "kupemphera mosalekeza" (Mach. 1:14; fanizilani 3:1; 6:2-4; 10:9).

Pemphero silimangosintha chabe nyengo, koma limasinthanso iye amene apemphera. Munthu wina obweretsa kusintha otchedwa Martin Luther, adamvetsetsa kufunikira kwake kwa pemphero. Zimanenedwa za iye kuti tsiku lina analankhula mokuwa, "Ndili ndizambiri zofunika kuchita lero moti kwa maola atatu woyambirira ndikhala ndikupemphera!" Momwemonso, pemphero likhale choyambirira pamoyo wa Mbusa aliyense wa Chipentekoste.[4]

---

[2] Kupeza zochuluka pazakufikira otaikawo, onani Mutu 37: "Kulalikira Otayika."

[3] Kupeza zochuluka pautumiki wa kalikidwe ka Mbusa wa Chipentekoste, onani Mutu 16: "Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu."

[4] Kupeza zochuluka paza mbusa wa Chipentekoste wamoyo wapemphero, onani Mutu 8: "Kufunikira Kwa Pemphero."

Kugwiriziza zikhulupiliro za Chipentekoste

Njira yachisanu ndi chimodzi ndiyoti Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuyesetsa kugwiriziza zikhulupiliro za Chipentekoste mu utumiki wake. Zikhulupiliro za Chipentekoste ndizokhulupirira zomwe timaikilapo mtima kwambiri ndi kuziperekako ndipo zimenezi zimafotozera munthu wachipentekoste weniweni. Mfundo zitatu zofunikira kuti Mbusa wa Chipentekoste asunge kapena kuziteteza ndi monga kudzipereka ku chiphunzitso choonadi cha Baibulo, kudzipereka kwathunthu kwa Mulungu ndi cholinga Chake, komanso kukhala otseguka kapena watcheru kukuyenda kwa Mzimu wa Mulungu.

Kukhala watcheru kapena womasuka kukuyenda kwa Mzimu wa Mulungu kukuphatikizapo kutsindika pakuwaona okhulupirira akubatizidwa mwa Mzimu Woyera.[5] Yesu komanso ndi atumwi adatsindika kufunikira kwa chimenechi. Asanabwelere kunka kumwamba, Yesu analamulira ophunzira otsatira Iye, "Musachoke mu Yerusalemu, koma mudikire mphatso imene Atate wanga analonjeza...koma posachedwapa inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera" (Mach. 1:4-5; fanizilani Luka 24:49). Patapita zaka zingapo, Paulo anakumana ndi ophunzira khumi ndi awiri aku Aefeso, funso lake loyamba kwa iwo linali loti, "Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?" (Mach. 19:2).

Yesu ndi atumwi anatsindika kuti ophunzira onse abatizidwe mwa mzimu Woyera chifukwa anadziwa ichi kale kuti chiwapatsa mphamvu kukhala mboni za Khristu "mu Yerusalemu, mu Yudeya monse, mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko" (Mach. 1: 8).

Kukonzekeretsa Anthu a Mulungu ku Ntchito ya Utumiki

Potsiliza, mbusa wa Chipentekoste ayenera kuika poyamba kusula anthu a Mulungu kuti akatumikire. Mbusa wa Chipentekoste wanzeru amamvetsetsa kuti china mwa zochita zake monga Mbusa ndi "kuti akonzekere oyera mtima [akhristu] kuntchito ya utumiki" (Aefeso. 4:12). Izi zikutanthauza kuti inuyo ngati abusa mukuyenera kuchita moposera kusamalira nkhosa chabe, koma mukuyenera kuwaumba anthu a Mulungu kuti akhale mamembala ogwiritsidwa ntchito

[5] Kupeza zochuluka za Makhalidwe a Chipentekoste, onani Mutu 10: "Amalimbikitsa Choonadi cha Chipentekoste"; Mutu 11: "Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekoste"; ndi Mutu 12: "Amayamikira Cholowa cha Chipentekoste."

aufumu. Choncho muonetsetse kuti kupanga ophunzira chikukhala chinthu chofunikira pautumiki.[6]

KUTSATIRA ZOFUNIKIRA ZA UTUMIKI

Titatha kuwona zinthu zisanu ndi ziwiri zofunikira abusa a Chipentekoste, muyenerano kupanga chisankho tsopano kuzitenga ngati zanuzanu. Ndi chinthu china kuwerenga za zofunikirazi mu buku ndipo ndichinanso kulora Mzimu wa Mulungu kuti azilembe pamtima wanu. Kuti ichi chikakhale chikuchitika, mukuyenera kudzipereka ku ndondomeko yakutembenuza mfundozi kukhala zofunikira kenako kutembenuza zofunikirazi kukhala zochitika mu utumiki. Tiyeni tione ndondomeko iyi.

Kukhazikitsa Zofunikira

Umayamba ndondomekoyi pozindikira kuti kukhala Mbusa wa Chipentekoste oyenereka ndi odziwa kumafunikira kuchitapo kanthu. Kutumikira koyenera ndi kudziwa ndipamathero paulendo wautali. Monga momwe zimakhalira ndi ulendo wina uliwonse, ulendo uwu umayambanso ndikusankha kothera kwake. Umapitilira pakukonza ndikuyenda mu dongosolo la momwe mutakafikire ku mapeto. Kuti mukakhazikitse zofunikira zisanu ndi ziwiri za utumiki wanu ndi mmautumiki a mpingo wanu, mukufunikira kuzipereka ku ulendowu.

Mutha kuyamba ulendowu potenga zofunikira zisanu ndi ziwirizi ndikuzilemba mu kope lanu. Kenako muzigwiritsa mndandanda wazimenezo ngati mlozo wanu wazopemphelera tsiku lililonse. Pamene mupemphera tsiku lililonse, mfunseni Mulungu kuti akhazikitse Mfundo zam'Baibulo zimenezi mkati mwa mzimu wanu. Mukachita zimenezi, kusintha kudzachitika pamoyo wanu. Mzimu Woyera adzayamba kulemba zofunikira zimenezi kunsi kwa mtima wanu. Mmalo mongokhala zinthu zolembedwa, zizakhalano zochitika zofunika mu utumiki.

Pamene inu mupemphera, muzifunse funso nokha, "Kodi zoyambirira zanga za utumiki panopa ndi ziti?" Zoyambirira zanu za utumiki panopa ndi zomwe inu nthawi zambiri mumatayapo nthawi ndi mphamvu zanu. Tchulani zoyambirira zimenezo. Kenako funsani, "Kodi zoyambirirazi zikukhala motani m'ndandanda

[6] Kupeza zochuluka pakutukula anthu a Mulungu, onani Mutu 16: "Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu" ndi Mutu 25: "Kulimbikitsa Thupi la Khristu."

wa zoyambirira za Yesu ndi atumwi? Kolingana ndikuzisanthula kwanu,muzifunsenso mafunso awa:

- Kodi ndikuchita bwino motani potumikira Mulungu pacholinga chake?
- Kodi ndikuchita bwino motani pokwaniritsa maitanidwe aMulungu pamoyo wanga ndi mpingo omwe ndikuutsogolera?
- Kodi ndikuchita bwino motani kufikira miyoyo yotaika ku malo komwe ndimapezeka ndi dziko lonse lapansi?
- Kodi ndikuchita bwino motani polalikira mau a Mulungu?
- Kodi ndikuchita mwamphamvu bwanji moyo wanga wapemphero ndi utumiki wa pemphero ku mpingo omwe ndikuutsogolera?
- Kodi ndikuchita bwino motani polimbikitsa zikhulupiliro zokhazikika za Chipentekoste mu mpingo wanga?
- Kodi ndikuchita bwino motani kukonzekeretsa anthu a Mulungu ku utumiki?

Lembani mayankho anu mu kope lanu. Tsopano zifunseni funso, "Kodi ndingapange chiyani mosiyana kuti ndithe kukwaniritsa chilichonse cha zofunikirazi m'moyo mwanga ndi utumiki?"Mobwerezanso, lembani mayankho anu mu kope, ndipo mupitilize kuzipempherera tsiku lililonse.

Kukwaniritsa Zofunikirazo

Pamene inu mwazitenga zofunikira zoyambirira za utumiki monga zanu, muyambe kuzichita mu utumiki wanuwo ndi mautumiki ena ampingo. Kuti mukwaniritse zimenezi muyenera kugwiritsa ntchito njira zingapo:

1. Chulukitsani kumvetsetsa. Mukuyenera kuchulukitsa kumvetsetsa kwanu pa zimene Baibulo limaphunzitsa pa chofunikira choyambirira chilichonse cha utumiki mwa zisanu ndi ziwiri. Mukhoza kuchita izi pofufuza malembo ndikufunafuna kuzindikira pa mitu imeneyi. Yesu akutilangiza ife kuti "Tisanthule Malembo mwakhama" nkufufuza kwathu kwa choonadi (Yohane 5:39). Pamene muwerenga, dzifunseni nokha, "Kodi Mzimu akunena chiyani kwa ine?" Lembani zomwe mwazindikirazo mu kope. Ngati nkotheka, mufunikira kupeza ndikuwerenga mabuku ena pa mitu imeneyi.[7]

[7] Buku lofotokozera bwino za cholinga cha Mulungu ndilotchedwa *Chiphunzitso cha M'baibulo cha Utumwi, lolembedwa ndi* Paul York, lotsindikizidwa ndi a Africa's Hope Discovery Series.

Njira ina yochulukitsira kumvetsetsa kwanu za mitu imeneyi ndikulalikira ndi kuphunzitsa pafupipafupi za zimenezi. Njira imeneyi ya kachitidwe siidzangowonjezera kumvetsetsa kwanu kokha kwa mitu, koma kuti idzakonzekeretsa mamembala anu kufika pa mlingo wina, komanso mkachitidwe ka zofunikira m'moyo wa mpingo.

2. Kukhala ndi dongosolo. Mudzayenera kukhala ndi dongosolo la momwe mutachitire zofunikirazi mu utumiki wanu ndi mautumiki ampingo. Kuti muchite zimenezi mukufunika kuchulukitsa kumvetsetsa kwa mpingo pa chofunika choyambirira chilichonse mwa zisanu ndi ziwirizi. Mukhoza kuyambapo poyankha mafunso otsatirawa:

- Ndichitenji kuti ndiutsogolere mpingo wanga kuti utumikire bwino cholinga cha Mulungu?
- Ndichitenji kuti ndikwaniritse maitanidwe a Mulungu pamoyo wanga ndi pampingo pamene wandiitana kuti nditsogolere?
- Ndichitenji kuti nditsogolere mpingo kuchita mwamphamvu kufikira miyoyo yotaika?
- Ndichitenji kuti ndilalikire ndi kuphunzitsa bwino mau a Mulungu mumpingo?
- Ndichitenji kuti ndilimbikitse pemphero mumpingo?
- Ndichitenji kuti ndiutsogolere mpingo kukhala wa Chipentekoste weniweni ndimmachitidwe ake?
- Ndichitenji kuti ndikakonzekeretse bwino anthu a Mulungu ku utumiki?

Lembani mayankho anu mu kope ndikumawaona mosanthula pafupipafupi.

3. Pangani kuti dongosolo lanu ligwire ntchito. Izi zikutanthauza kuti muyenera kupita chitsogolo nkuyamba kuchita ndikutsata njira zimene mwaziika kale. Pamene inu mupita chitsogolo ndi dongosolo lanu, muzikhala ndi nthawi yosanthula ndikuwunikanso kuti zikuyenda motani. Ngati nkofunikiranso, mutha kusintha dongosolo lanu lija.

Kumbukirani, chipambano sichimabwera mophweka. Chipambano kuti chioneke chimatenga kanthawi, ndipo pamene zovuta zibwera mudzafunika kupilira. Ngati mudzachita ichi munthawi yake, mpingo wanu udzayamba kusintha. Mpingowo udzakhala wamphamvu monga momwe Khristu amafunira kutiukhalire. Mau amtumwi akulimbikitseni: "Koma tisaleme pakuchita zabwino; pakuti pa nyengo yake tidzatuta tikapanda kufooka" (Agalatiya. 6:9).

Mbusa aliyense wa Chipentekoste mu Afirika akuyenera kuika zoyambirira zake za utumiki kuti zigwirizane ndi izo za Yesu ndi atumwi. Abusawa alore kuti zoyambirira zimenezi zitsogoleremautumiki awo. Ngakhale kuti ndondomekoyi ikhoza kukhalayolimbilapo, ndiyoyenera kuchita khama. Kudzera nkudzipatulira kwa Khristu, kudzipereka ku chifuniro cha Mulungu, ndikufulumizitsa kwa mphamvu ya mzimu Woyera, Mbusa wa Chipentekoste akhoza kukwaniritsa zolinga za utumiki.

~ Mutu 6 ~

Zofunikira Zoyambirira Pa Moyo

Ana aamuna a amai anandikwiyira, anandisungitsa minda yamipesa; koma munda wangawanga wamipesa sindinausunge" (Nyimbo Ya Solomoni 1:6). Awa ndi mau a chisoni kuchokera kwa mtsikana waku Sunemu. Anali wotanganidwa kwambiri kusamalira minda ya ena kufikira kuti sadasamalire wake. Komabe, Iye samayankhula za minda yamipesa yooneka; koma amayakhula za moyo wake. Anayikiza nthawi yochuluka mwa ena kufikira kuti moyo wake tsopano wachuluka ndi namsongole.

Mwachisoni, chikhalidwe chomwechi chitha kufotokozera miyoyo ya abusa ambiri a Chipentekoste mu maiko a Afirika lero lino. Ataya nthawi yambiri kusamalira zokhudza utumiki, kutumikira zosowa za ena, koma alephera kusamalira iwo eni. Zotsatira zake onse avutika. Moyo wao wauzimu wauma, komanso mipingo yomwe akutsogolera yafooketsedwa.

Paulo anasankha Timoteo kuti asamalire mpingo wa ku Aefeso. Kenako analemba kalata kwa mnyamatayu, kumuchenjeza, "Udzipenyerere wekha, ndi chiphunzitsocho. Uzikhala mu izi; pakuti pochita izi udzadzipulumutsa iwe wekha ndi iwo akumva iwe" (1 Tim. 4:16). Paulo potero akumulangiza Timoteo, kuti iye asangosamalira zautumiki wake okha poyera, komanso ku malo ake a mseri. Mbusa wa nzeru samangoona kufunikira kwa utumiki wake kwa ena, monga zanenedwa mu mutu 5, komanso iwo aona kufunikira kwa kuzisamalira iwo eni.

Mutu uwu tiona zinthu zisanu ndi chimodzi zofunikira kwambiri kwa Mbusa wa Chipentekoste.

KUFUNIKIRA KWA KUDZIWA KHRISTU

Pamwamba pa zonse, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuika koyambirira ubale wake ndi khristu. Asanapangitse ena kuti amudziwe Iye, iwo eni ayenera kumudziwa Iye bwino lomwe. Kodi munthu angafotokozere bwanji za wina kwa munthu amene iwosakumudziwa?

Ngati Mbusa wa Chipentekoste, uyenera kudziwa Khristu mu zonse, mwa nzeru komanso m'zochitika zake. Munjira ina,umvetsetse kuti Khristu ndi ndani ndi zomwe Iye wachita. Ndikuti unakumana naye, ndikukhala paubwenzi wapafupi ndi Iye.

Kumudziwa kuti Iye ndi Ndani

Kudziwa Khristu mwa nzeru ndiko kudziwa choonadi chokhudza Iye. Ndi kumvetsetsa zomwe Baibulo limakamba zokhudza kuti Iye ndi Ndani komanso chifukwa chomwe Iye anabwera pa dziko lapansi. Baibulo limaphunzitsa zotsatirazi zokhudza Khristu kuti ndi ndani:

- Iye ndi Mau a Mulungu a muyaya, Wolenga wa zinthu zonse (Yohane 1:1-4).
- Iye ndi Mulungu woonekera m'thupi (1 Timoteo 3:16).
- Iye ndi, "Mesiya, Mwana wa Mulungu wamoyo" (Mateyu 16:16).
- Iye ndi "Njira, ndi choonadi, ndi moyo," njira yokhayo ya kwa Atate (Yohane 14:6).

Baibulo limatiuzanso chifukwa chomwe khristu anabwera kudziko lapansi:

- Iye anadza "kudzafunafuna ndi kupulumutsa otayikawo" (Luka 19:10; fanizilani 1 Timoteo. 1:15).
- Iye anadza "kutumikira, ndi kupereka moyo wake ngati nsembe chifukwa cha anthu ambiri" (Marko 10:45; fanizilani Yohane 12:27; Tito 2:13-14).
- Iye anadza "kuti awononge tchito za mdierekezi" (1 Yohane 3:8; fanizilani Ahebri 2:14).
- Iye anadza "kuti [ife] tikhale ndi moyo, ndi kukhala naowochuluka" (Yohane 10:10).

Kumudziwa Iye Pawekha

Pamene zili zofunikira kuti Mbusa wa Chipentekoste adziwe kuti Yesu ndi ndani komanso chifukwa ninji Iye anabwera, koma izi sizokwanira. Ngati Mbusa wa Chipentekoste, uyenera kumudziwa Khristu pawekha. Uyenera kuti unakumanapo ndi Ambuye pawekha, ndi kuti uli pa ubwenzi ndi Iye womwe ukupitirirabe.

Paulo anayakhula za kufunikira uku m'moyo wake womwe. Analemba kwa okhulupirira a kwa Afilippi, "Kuti ndimzindikire Iye, ndi mphamvu ya kuuka kwake, ndi chiyanjano cha zowawa zake, pofanizidwa ndi imfa yake" (Afi. 3:10). Kukhumbitsitsa kwa Paulo kuti adziwe Khristu kunali kwakukulu kufikira kuti anali wokonzeka, osati kungogonjetsa kokha ndi Iye, komanso kuti ayanjane ndi Iye m'zowawa zake. Adali wokonzeka kuti afe chifukwa cha Iye. Mbusa wa Chipentekoste ayenera kugawana ndi chokhumba cha Paulo pa kudziwa Khristu.

Kuyamba Kumudziwa Khristu

Utha kufunitsitsa kudziwa Khristu kufunikira kwake mu njira zitatu:

1. kudzera mkukumana Naye. Munthu koyamba amadziwa khristu kudzera mkukumana naye. Izi ndizochitika kwa aliyense, ngakhale mbusa wa Chipentekoste. Saulo waku Tariso anadziwa zokhudza Khristu; komabe, sadamudziwa Iye pa iye yekha kufikira atakumana naye pa njira ya ku Damasiko (Machitidwe 9:1-9). Pamenepo, Saulo adafuula, "Ndinu yani Mbuye?" Yesu anayakha, "Ndine Yesu amene umlondalonda" (v. 5). Moyo wa Saulo unatembenuka. Anamdziwa Khristu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi wake. Mkanthawi kochepa, munthu wozunza mpingo, woopsa anakhala owupititsa patsogolo wankulu.

Pakuonanso zomwe zinam'chitikirazi, Paulo akulemba,"Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano" (2 Ako. 5:17). Yense amene amafuna kukhala Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuyambira paemenepa. Yesu adalengeza, "Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona ufumu wa Mulungu" (Yohane 3:3).

2. Kudzera m'Mau a Mulungu. Njira ya chiwiri yomwe Mbusa wa Chipetenkoste atha kudziwa Khristu bwino lomwe ndi kudzera mukukumana naye mu Baibulo— makamaka m'mauthenga abwino komanso m'makalata.

Mauthenga abwino amanena za moyo wake, ntchito zake, ndi ziphunzitso zake. Makalata amafotokozera matanthauzo ake. Pakuwerenga mauthenga abwino, mutha kuyenda miseu ya fumbi yaku Galireya ndi Yesu. Mutha kukhala pamapazi ake ndi kumvetsera ziphuzitso zake. Mutha kuima ndikumuona Iye akufa pa mtanda. Ndipo mutha kuyang'ana m'manda a Mpulumutsi wanu ndikumva Angelo akukuwa, "Iye Sali muno. Wauka kwa akufa!"

Mbusa wa chinyamata wa Chipentekoste adanenapo kwa ine, "Ophunzira a Yesu adakhala zaka zitatu alikuyenda ndi Iye ndikuphunzira kuchokera kwa Iye. Miyoyo yao inasandulizika. Inenso ndichita chimodzimodzi. Mu zaka zitatu ndikhala ndikuwerenga ndi kuwerenganso mobwereza Mauthenga Abwino anayi." M'choonadi cha kuzipereka kwake, wolalikira wachichepereyu anatha zaka zitatu akuwerenga mauthenga abwino. Ola pa ola linathera kuzikhuthula pa mbiri ya Yesu. Zitatha izi, moyo wake ndi utumiki wake sunakhalenso chimodzimodzi.

3. Kudzera m'pemphero. Njira yachitatu momwe mbusa wa Chipentekoste atha kudziwa Khristu ndi kudzera mu pemphero. Baibulo limayakhula za mitundu yambiri ya mapemphero, kuphatikizapo, zopempha, kulapa, zopembedzera, kuyamika, ndi kupemphera mu uzimu. Komabe, mtundu wa pemphero womwe umthandizire Mbusa kudziwa bwino Khristu ndi pemphero lachiyanjano. Yakobo anayankhula za mtundu wa pempherowu. "Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu. (Yakobo 4:8). Nayenso Mose amachita mapemphero achiyanjano. Baibulo likuti iye amayakhulana ndi Mulungu "kopenyana maso, monga munthu alankhula ndi bwenzi lake" (Eksodo. 33:11).

Maria, mlongo wake wa Marita, ndi fanizo labwino la mtundu wa pemphero uwu. Pamene Yesu anafika kunyumba kwake, iye anakhala pa mapazi a Iye chifupi kumvetsera bwino kumau amene Iye amayankhula. Mlongo wake adandaula, pomunena iye kuti adali waulesi. Komabe, Yesu anayamikira Maria, kuti, "[Iye] anasankha dera lokoma limene silidzachotsedwa kwa iye" (Luka 10:38-42). Kufunitsitsa kuti umudziwe Yesu chikhale chinthu chofunikira cha mbusa aliyense wa Chipentekoste. M'chitidwe uwu ukhudza moyo wake komanso utumiki wake.

KUFUNIKIRA KWA KUYENDA MU MZIMU WOYERA

Mbusa wa Chipentekoste asamangofuna kudziwa Khristu kokha, koma iye afunitsitse kuyenda ndi kukhala mu Mzimu Woyera. Paulo analangiza Akhristu a

ku Agalatiya "Ngati tili ndi moyo ndi Mzimu, ndi Mzimunso tiyende" (Agal. 5:25).

Zomwe Zimatanthauza Kuyenda mu Mzimu

Kuyenda mu Mzimu zimatanthauza zinthu zosachepera zitatu:

1. Kudzazidwa ndi Mzimu. Choyamba, kuyenda mu Mzimu zimatanthauza kuti kudzazidwa ndi Mzimu (Machitidwe 1:4-8). Mu mau ena, tisanayende mu Mzimu, aliyense ayenera kubatizidwa ndi Mzimu Woyera onga analili ophunzira pa Tsiku la Pantekoste (Machitidwe 2:1-4). Atatha iwo kulandira Mzimu, ophunzirao adayamba kukhala ndi kutumikira mu mphamvu ya Mzimu. Buku la Machitidwe limanena nkhani yabwino za utumiki wa mphamvu ya Mzimu. Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kukhala ndi chochitika ichi.

2. Kutsogozedwa ndi Mzimu. Chachiwiri, kuyenda mu Mzimu ndi kutsogozedwa ndi Mzimu. Mbusa wa Chipentekoste, ayenera kusunga khutu lake likhale lotseguka ku liwu la Mzimu Woyera. Kenako, pamene Mzimu ayankhula, ayenera kumvera. Izi ndi zomwe Yesu anachita. Koyamba anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Kenako anatsogozedwa ndi Mzimu (Luka 3:21-22 ndi 4:1). Paulo ndi gulu lake la atumwi anatsogozedwanso ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 16:6-10). Izi ndi zoonadinso kwa Mbusa wa Chipentekoste lero lino. Monga Yesu ndi Paulo, iwo ayenera kutsogozedwanso ndi Mzimu wa Mulungu.

3. Kutumikira mu Mzimu. Chotsilizira, kuyenda mu Mzimu kutanthauza kutumikira mu mphamvu ya Mzimu. Yesu analonjeza, "Komatu mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko" (Machitidwe 1:8). Izi ndi zomwe zinachitika kwa Yesu komanso atumwi. Iwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndikuyamba kutumikira mu mphamvu ya Mzimu (chitsanzo, Luka 3:21-22 ndi 4:14; Machitidwe 4:31-33). Pamene muyenda mu Mzimu, inunso mutha kuyembekezera kuti Mzimu Woyera apereka mphamvu ku utumiki wanu.

Mungayende bwanji Mu Mzimu

Funso nali, ngati Mbusa wa Chipentekoste, uyenera kuchitanji kuti uwonetsetse kuti ukukhala komanso kuyenda mu Mzimu? Choyamba, monga zafotokozeredwa mwambamu, uwonetsetse kuti wadzazidwa mu zenizeni ndi Mzimu Woyera. Pamene wadzazidwa ndi Mzimu utha kuyembekeza zizindikiro

ziwiri zomwe baibulo limanena: choyamba ndi chakuti umayankhula ndi malilime ena monga Mzimu akuyankhulitsira (Machitidwe 2:4; 10:44-46; 19:6). Chachiwiri ndichakuti umalandira mphamvu ya Mzimu kuti uchitire umboni za Khristu (Machitidwe 1:8; 4:31).

Pamene wadzadzidwa ndi Mzimu Woyera, uyenera kusunga mtima wako ku machitachita a Mzimu. Izi ndi zomwe Akhristu amachita m'buku la Machitidwe. Mnthawi ya msonkhano wao waukulu ku Yerusalemu, atumwi akuluakulu adapanga chisankho zokhudza kuphatikiza okhulupirira amitundu mu mpingo. Adayamba kalata wao ndi mau akuti, "Pakuti chinamkomera Mzimu Woyera ndi ife" (Machitidwe 15:28). Amafuna kuti owerengawo adziwe kuti adamvera liwu la Mzimu chisankho chisanapangidwe. Chikhalidwe chimodzi chomwe chingakuthandizire kuti muyende ndikukhala mu Mzimu ndikukhala ndi nthawi tsiku lililonse kupemphera mu Mzimu Woyera (Aroma 8:26-27; Aefeso 6:18).[1]

KUFUNIKIRA KWA KUKULA NDI KUZITUKULA WEKHA

Kuphatikizapo kudziwa Khristu ndi kuyenda mu Mzimu, mbusa wa Chipentekoste ayenera kufunitsitsa kukula ndi kuzitukula. Iye achilimike nthawi ndi nthawi kuti akhale wapamwamba chifukwa cha Ambuye.

Kufanizira moyo ku mchitidwe wothamanga, Paulo akuwauzitsa Akhristu a ku Akorinto kuti atsate kupambana. Adawakumbutsa iwo, "Kodi simudziwa kuti iwo akuchita makani a liwiro, athamangadi onse, koma mmodzi alandira mfupo?" kenako anawalimbikitsa iwo, "Motero thamangani, kuti mukalandire" (1 Akorinto. 9:24). Mu njira yomweyi anawalimbikitsa Akolose, "Chilichonse mukachichita, gwirani ntchito mochokera mumtima, monga kwa Ambuye" (Akolose 3:23).

Chikhalidwe chakupambana ichi sichochita kutengera kwa makolo kapena kuchita kuyikizidwa ndi pakusanjika kwa manja ayi. Kukwaniritsa chipambano mu utumiki kumafuna chindunji, kutsimikizika ndi kuziletsa. Kutsata chipambano sikuyesera kukhala oposa winawake. Koma, ndikukhala woposa mmene ungakhalire mkutumikira Ambuye.

[1] Pa zambiri zokhudza moyo wapemphero wa mbusa wa Chipentekoste, onani mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

Dera limodzi lomwe Mbusa wa Chipentekoste ayenera kutsata chipambano ndi chikhalidwe chake pakuwerenga. Mwatsoka,komabe, pali chikhalidwe mkatimkati mwa abusa a Chipentekoste chakunyoza kuwerenga. Pamene akuyika pamwamba chidziwitso choikizidwa, iwo amayang'anira pansi chidziwitso chochita kupeza. Baibulo, komabe, limaphunzitsa kuti, "Mtima wa wozindikira umaphunzira; khutu la anzeru lifunitsa kudziwa" (Miyambo 18:15).

Choncho, ngati mbusa wa Chipentekoste okhulupirika, uyenera mosatopa kufunitsitsa kuchuluka, chidziwitso cha malembo. Nthawi yomweyo funitsitsa kukhala wodziwa bwino za zomwe zikuchitika mdera. Pamenepo udzatha kuphatikiza zonse ziwiri, moyera kutsatira ma uneneri a choonadi cha Baibulo ku zomwe zikuchitika. Komanso, uyenera kupanga chikhalidwe chakuwerenga mabuku abwinokuchokera kwa olemba odziwika bwino. Mchitidwe uwu uchulukitsa luso lakaganizidwe kako. Kupambana mu kuwerenga kuthandizira kubala chipambano mu utumiki.

KUFUNIKIRA KWA KUZISAMALIRA

Kanthawi kena, Mbusa wina wa Chipentekoste amakumana ndi kutopa kopyola muyezo komanso ma ululu mthupi. Anapita kwa dotolo ndi mantha akuti wagwida ndi nthenda yoopsa. Komabe, atatha kumuyeza, dotolo anamuuza kuti zizindikiro zake zinayamba chifukwa cha kupanikizika. Dokotala anamuthandiza kuti Mbusayi azikakhala ndi nthawi yopuma ndi kudya chakudya cha thanzi.Zinagwira ntchito! Posakhalitsa mbusayo nyonga zake zinabwerera mu utumiki.

Abusa a mu Afirika amadziwika kuti ndiolimbika pa ntchito. Izi ndi zabwino. Komabe, akhale osamala pamene akuyesera kukhala chilichonse kwa aliyense. Mbusa wotopa atha kukhala ngongole ku banja lake komanso ku mpingo wake. Kupanikizika kutha kuwononga kuthekera kwa mbusa kukupemphera, kuwerenga, ndi kulalikira. Zithanso kukhudza khalidwe lao pagulu; kuwapangitsa iwo kuoneka osokonekera komanso osakhudzidwa ndi nyengo ya wanthu. Zotsatira zake, zitha kubweretsa kusakhutitsidwa kwa anthu, kulenganso mavuto ochuluka pa mbusa.

Abusa ambiri a Chipentekoste amathawa nthawi yopuma. Amaganiza kuti akatenga nthawi kupuma, akukhala osakhulupirika ku maitanidwe ao. Komabe, Yesu, anamvetsetsa kufunikira kwa kupuma. Kamodzi anauzapo ophunzira ake

kuti, "Idzani inu nokha padera ku malo achipululu mupumule kamphindi" (Marko 6:31).

Mbusa wamachawi ayenera kukumbukira kuti Mulungu mwini anapuma tsiku lachisanu ndi chiwiri la kulenga (Gen. 2:2). Anachita izi, osati chifukwa anali atatopa, koma kuti akhale chitsanzo kwaanthu onse. Yesu anati, "Sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha Sabata" (Marko 2:27). Mulungu anapereka Sabata ngati njira yoti anthu ake alemekeze Owalenga, komanso ngati nthawi yoti atenge mphamvu zina zofunikira kuti akumane ndi zofuna za moyo. Ngati mfundo ya Sabata iphwanyidwe, zibweretsa kupelewera mu utumiki.

Mbusa wa Chipentekoste ayerenera tsono kupatula tsiku limodzi msabata iliyonse pakupuma ndikuzibwezeretsa. Iye adziwitse anthu ake kuti ili ndi tsiku lomwe Mbusa akupuma, Sabata lake. Mbusa ataye nthawi iyi mkuzisangalatsa ndikukondwera ndi wokondedwa wake ndi ana ake.[2]

KUFUNIKIRA KWA CHIYERO CHA IWE MWINI

Kankhani kena kanalembedwa mu nyuzi pepala lina kummawa kwa Afirika kukamba za mbusa wina wodziwika amene analekana ndi mkazi wake chifukwa cha khalidwe la mkazi lachigololo. Mbusayu anakana kumukhululukira mkaziyo ndipo anasankhakukwatiranso. Kuona zomwe Mbusayu wachitira mkazi wake, bambo wina anati kwa mkazi wake, "Ngati Mbusa walekana ndi mkazi wake, iwe ndiwe ndaninso?" Iyenso anasiya mkazi wake kutsata mkazi wina. Ngati mbusa, zochitika zako zimakhudza machitidwe aiwo ukuwatsogolera, kuzabwino kapena kuzoipa.

Monga mbusa wa Chipentekoste Mulungu akukuyitanira ku moyo wachitsanzo. Petro akulemba, "Komatu monga Iye wakuitana ali woyera mtima, khalani inunso oyera mtima,m'makhalidwe anu onse; popeza kwalembedwa, Muzikhala oyera mtima, pakuti Ine ndine woyera mtima" (1 Pet. 1:15-16). Paulo analemba kuti woyang'anira ayenera kukhala moyo "Wopanda chilema, mwamuna wa mkazi mmodzi, wodzisunga, wolongosoka, …wosati woledzera" (1 Tim. 3:2-3). Anaonjezeraponso kwawoyang'anira, "iwo akunja adzakhoza kumchitira umboni wabwino" (v. 7). Kwa Tito, mtumwi anati pakuti

[2]Pa zambiri zokhudza kuzisamalira-wekha, onani mutu 13: "Moyo-Woyang'aniridwa bwino."

woyang'anira "ayenerakukhala wopanda chilema…wokonda zokoma, wodziweruza, wolungama, woyera mtima, wodziletsa" (Tito 1:7-8).

Mu Afirika, abusa amapatsidwa ulemu waukulu. Amakhudza anthu molunjika ndi mosalunjika. Amakhudza miyoyo yaomwachindunji ndi mau-pa zomwe akunena. Amakhudzanso miyoyo yao mosalunjika ndi moyo wao-pa zomwe amachita. Zomwe abusa amachita nthawi zambiri ndi zomwe zimabweretsa kukhudza kuposa zomwe amanena. Membala wina adauzapo Mbusa wake, "Zomwe mmachita zimayankhula mokweza sindingathe kumva zomwe mukunena." Choncho, ngati Mbusa wa Chipentekoste, uyenera kupanga moyo wakukhala mu chiyero kukhala chinthu chofunika kwambiri pa Iwe.

KUFUNIKIRA KWA KUSAMALA ZA NTHAWI

Achipentekoste amalemekeza kulambira kodzipatula komanso kudzikhuthula. Amayembekezera kuti Mzimu alowererepo mosachita iwo kuchalira zoti Mzimuyo achite. Zikhalidwe izi ndi zabwino, ndipo siziyenera kusiyidwa. Komabe, mbusa wa Chipentekoste asagwiritse ntchito izi ngati chifukwa chakulephera kusamalira nthawi. Monga uli mdindo pa ndalama zomwe Mulungu waikiza mmanja mwako, chomwecho, ndiwe mdindo panthawi yomwe Mulungu wakupatsa. Choncho,uyenera kudzipereka wekha ku kasamalidwe kanthawi kabwino.

Abusa ena ndi opanda khalidwe ndi nthawi yao, komanso amakonda kuchedwa ku mikumano ndi misonkhano. Abusa otere amaika dongosolo lolakwika lotsatidwa mmipingo yomwe akutsogolera. Chikhalidwe chakusasamala ichi, chimachepetsa ungwiro wao ndi wanthu. Chimakhala mbali imodzi la ndogosolo la mpingo komanso kulepheretsa kupita patsogolo.

Kumbali ina, kusamalira nthawi kwabwino kumakuthekeretsa kuti utsogolere mpingo mwabwino kwambiri. Umakhala ndi kuthekera kokhala ndi nthawi ya kuphunzira mau, ntchito zamu ofesi, kuyendera, kupereka uphungu, ndi zina zapabanja. Kusamalira bwino kwa nthawi kumaphatikizapo zinthu zomwe ukwaniritse patsiku, kukonza dongosolo la zomwe zichitike, kukonza ntchito zofunika kuti zichitike molingana ndi kufunika kwake ndi changu chake, ndi kukonzeratu nthawi yoti ntchito iliyonse ichite.

Ngati mbusa wa Chipentekoste, uyenera kukhala ndi cholinga cha mmene ukhalire mmoyo ndi kuchita utumiki. Uyenera kukhazikitsa mwadaladala zinthu zofunika kwambiri pa moyo wako. Uyenera kenako mozindikira kuyamba kukhala molingana ndi zofunikirazo. Ngati uchita zinthu izi udzadalitsika, limodzi ndi anthu amene uwatsogolera.

~Mutu 7 ~

Zofunikira Zoyambirira pa Banja

Mbusa wampingo wina waukulu m'tawuni ku mmawa kwa Afirika anapereka nkhani yokhudza agogo ake amuna. Kwa zaka zambiri agogo ake anatumikira mpingo wa Chipentekoste.Komabe, tsiku linadza lomwe adasiya banja lake ndi chikhulupiriro chake ndikuzitengera yekha akazi atatu. Chifukwa cha kulephera komvetsa chisoni kotere, palibe ndi mmodzi mwa ana ake amene anatsata Ambuye. Ndithu palibe, kupatula mayi ake a Mbusayu. Mbusa tsopano akuchitira umboni "Ndine chipatso cha kukhulupirika kwa mayi anga. Ndi iwo amene anandikhudza ine kuti nditsate Ambuye." Lero, Mbusa ameneyu ndiodziwika bwino ndi ziphunzitso ndi kulalikira zokhudza mabanja.

Choonadi chokhumudwitsa m'chakuti inde ngakhale abusa a Chipentekoste nthawi zina amavutika m'mabanja mwao komanso ndi ana ao. Chifukwa cha ichi, ayenera kuika kusamala kwa maubwenzi am'mabanja ao kukhala chinthu chofunikira kwambiri. Kwa Mbusa, kukhala opambana mnyumba mwake ndi kukhala opambana mwaubwino; kulephera ndi kulephera kwathunthu. Mitu iwiri mbuyomo yakamba machitidwe a Mbusa wa Chipentekoste pa utumiki komanso moyo wake. Mutu uwu ukamba za kufunikira kwa mabanja ao.

MAUBALE M'BANJA

Baibulo limayankhula za ubale wa mbusa ndi Banja Lake. Paulo adalemba zokhudza mbusa motere, "Woweruza bwino nyumba yake ya iye yekha, wakukhala nao ana ake omvera iye ndi kulemekezeka konse." Kenako mtumwiyu akufunsa mokometsera, "Koma ngati munthu sadziwa kuweruza nyumba yake ya iye yekha, adzasunga bwanji Mpingo wa Mulungu?" (1 Tim. 3:4-5). Malangizo a baibulo kwa azibambo, amayi komanso ana amagwiranso ntchito kwa mbusa m'nyumba yake (Gen. 2:24; Marko 10:6-9; 1 Akori. 11:3; Aefeso. 5:22-33; 6:1-4; Akolose 3:18-21; 1 Petro 3:1-7).

Dongosolo la Baibulo

Ngati Mbusa wa Chipentekoste, moyo wako wapanyumba ukhale molingana ndi dongosolo la malembo. Pamene chikhalidwe chikutsutsana ndi malembo, nthawi zonse udzipereke kuchotsilizirachi, kuonetsetsa kuti machitidwe ako ndi wokondedwa wako ali mu chiyanjano chonse ndi ziphunzitso za mau a Mulungu.

Mwachitsanzo, maiko ambiri mu Afirika amamuona mwamuna ngati olamulira amene sayenera kutsutsidwa ndi banja lake. Mau ake, kaya ndi opanda nzeru chotani asatsutsidwe. Komabe, Yesuadaonetsera utsogoleri wa mtundu wina osiyana. Kulankhula za Iye mwini adati, "Pakuti ndithu, Mwana wa Munthu sanadze kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la kwa anthu ambiri" (Marko 10:45).

Ambuye anakonzeratu mtundu wa utsogoleri omwe Iye akuyembekeza kwa iwe ngati mwamuna wa Chikhristu. Utsogoleri wako m'banja uyenera kutanthauzidwa ndi kudzichepetsa ndi kusazikonda chifukwa cha mkazi wako ndi ana. Paulo anatambasula pa mutu wa utsogoleri-wotumikirawu, kulimbikitsa amuna, "Kondani akazi anu, mongani Khristu anakonda Mpingo, nadzipereka yekha m'malo mwake" (Aefeso. 5:25).

Paulo anafotokozera mmene nyumba ya okhulupirira iyenera kukhalira: "Pakuti mwamuna ndiye mutu wa mkazi, monganso Khristu ndiye mutu wa Mpingo, ali yekha Mpulumutsi wa thupilo" (Aefeso 5:23). M'malo ena, mtumwi analemba, "Amuna inu, kondani akazi anu, ndipo musawawire mtima iwo. Anu inu, mverani akubala inu m'zonse, pakuti ichi Ambuye akondwera nacho. Atate inu, musaputa ana anu, kuti angataye mtima" (Akolose 3:19-21). M'malo abwino otere, banja lanu litha kukula ndipo ana anu kukondweranso.

Kudzipereka Mofanana

Baibulo limatiphunzitsa kuti ubwenzi pakati pa mwamuna ndi mkazi uyenera kukhala kwa kudzipereka mofanana. Paulo adalemba kuti amuna ndi akazi ayenera "Kumverana wina ndi mnzake m'kuopa Khristu" (Aefeso. 5:21). Ngakhale mwamuna ali mutu wa mkazi, ayenera, monga Khritsu, kudzipereka mofuna yekha kwa zosoweka za iye komanso modzichepetsa kumtumikira iye. Mkazi ayeneranso kuchita mofanana kwa iye. M'malo mozitsitsa ngati Mbusa, m'chitidwe odzichepetsa uwu ku banja lako umatukula mayimidwe ako mu Mpingo komanso kudera.

Chikondi ndi Kulemekezana

Kupitirira apo, ubwenzi ndi banja lako ukhale odziwika ndi chikondi ndi kulemekezana kofanana. Paulo akunena kwa amuna, "Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Mpingo nadzipereka yekha m'malo mwake" (Aef. 5:25). Kenako akuonjezera kuti, "Komanso inu, yense pa yekha, yense akonde mkazi wake wa iye yekha, monga adzikonda yekha; ndipo mkaziyo akumbukire kuti aziopa mwamuna" (ndime. 33). Chibwereza ndi choonanso; mkazi ayenera kukonda mwamuna wake, ndipo mwamuna ayenera kulemekeza mkazi wake. Pakuchita zinthu izi, banja la Mbusayo lidzakhala chitsanzo kwa ena.

Kukhala Weniweni

Kupitirira, ubale ndi banja lako ukhale ozikika pa zowona zenizeni. Izi zikutanthauza kuti uyenera kukhala munthu amene uli kunyumba zomwe uli poyera kapena kugulu. Uyenera kuonetsera chidwi choona mtima mu zomwe zikuchitikira okondedwa anukomanso ana. Pamene muli kunyumba, ana adzimva liwu la bambo ao kapena mayi wao, osati ngati olalikira amene ali kutali ndi zenizeni za miyoyo wao.

ZOVUTA ZA ABUSA ACHIKAZI

Liwu kwa abusa achikazi ndi mabanja ao liri mu dongosolo lake apa. Abusa achikazi omwe ali pa banja mu Afirika amazipezekeretsa okha pa malo apaderadera komanso ovuta. Mulungu waitana kuti atsogolere Mpingo; komabe, mu nkhani zokhudza m'nyumba mwao, Iye waitana kuti alemekeze amuna ao ndi kugonjera ku ulamuliro wao. Iyi itha kukhala nyengo yovuta kuti ayiyang'anire.

Kuphatikiza apo, zikhalidwe zambiri mu Afirika zimakaniza utsogoleri wa achizimayi, ngakhale, moyamikira, madera ambirikaonedwe aka kakusintha. Zotsatira zake, mipingo ina ndi yonyalanyaza kutsatira utsogoleri wa Mbusa wa mkazi kapenakumulora kuchita ntchito zina monga Mbusa.

Choncho ndizofunikira kwambiri kuti mwamuna wa Mbusayu athandizire mkazi wake mu utumiki wake. Nthawi zina, iye akhale ofunitsitsa mukudzichepetsa ndi kuthandiza iye mu njira zomwe zikuoneka zosiyana ndi machitidwe achikhalidwe. Mwa chitsanzo, nthawi zina, molingana ndi zofunika pa ntchito yake, mwamuna ayenera kudzichepetsa mofuna, ndi kudzilowetsa, ndi kuthandizamulimonse iye angathere. Kumbali inayo, Mbusa wa mkaziyo asagwiritse ntchito udindo wake pa utumiki kukhala zifukwa zakunyozera udindo wapakhomo kwa mwamuna wake ndi ana ake.

Izi zifunikira mlingo wapaderadera wakukhwima ndi kusinthasintha kumbali zonse za mbusa wachizimayi ndi mwamuna wake. Ayenera kuona ubale wao kukhala ofunikira kuposa china chilichonse, ndipo aphunzire kuyakhulana bwino wina ndi mzake.

KUYANG'ANIRA MOYENERA BANJA

Mbusa wa Chipentekoste asamangoyang'anira bwino mpingo wake okha, ayenera kusamalira bwino banja lake. Monga zaonedwa m'mwambamu, Paulo anamkumbutsa Timoteo kuti oyang'anira "Akhale oweruza bwino nyumba yake" (1 Tim. 3:4). Adalembanso nthawi ina kwa Tito, "wopanda chilema, mwamuna wa mkazi mmodzi, wokhala nao ana okhulupirira, wosasakaza zake, kapena wosakana kumvera mau" (Tito 1:6).

Udindo ofunikira uwu umaphatikizapo kutsogolera, kuteteza, ndi kusamalira mkazi wake ndi ana ake. Baibulo limaphunzitsa kuti mwamuna ayanjane ndi mkazi wake monga Khristu achitira ndi Mpingo (Aefeso 5:25-27). Mopitirira, iye ayenera kuyang'anira ana ake ndi kukhudzika kwa chikondi chomwecho chomwe atate ake akumwamba amamuyang'anira. Munthu wanzeru adapereka uphungu, "Phunzitsa mwana poyamba njira yake; ndipo angakhale atakalamba sadzachokamo" (Miyambo 22:6).

Ngati mbusa wa Chipentekoste, utsogoleri wako pa banja ukuphatikizapo kuchita zinthu zosachepera zitatu izi:

Kukula Moyo Wauzimu

Choyamba, uyenera kumakhudzidwa wekha ndi kukula kwa moyo wauzimu wa banja lako. Monga Yobu, uyenera kutsogolera banja lako pa zokhudza uzimu (Yobu 1:4-5). Njira imodzi yomwe mungachitire izi ndi kumakhala ndi nthawi yopembedza pafupi-pafupi ndi banja lako. Mu nthawi yopembedzayi, muyenera kuphunzitsa ana anu kupemphera, ndi kuwerenga komanso kuloweza malembo. Muonetsetse mopitirira apo kuti afike podziwa Khristu ngati Mbuye ndi mpulumutsi, ndikuti abatizidwa ndi Mzimu Woyera.

Kukula kwa iwe Mwini

Chachiwiri, uyenera kuyang'anira kuti banja lako likukula mu umwini. Inu ndi okondedwa anu mulunjike pakuumba ana anum'makulidwe akukhwima, kukhala Akhristu odzipereka, ndinso nzika zopindulitsa. Kuwonjezera apo, muphunzitse ana anu m'mene angachitire ndi ndalama. Pamene ana anu akukula ndi kukhala okhwima msinkhu, muwalore kuti iwo azithandizira mukusamalira chuma cham'nyumbamo. Mu njira imeneyi, atha kuphunzira kusiyanitsa pakati pa zokhumba chabe ndi zomwe zili zosowekera.

Kukula Muchikhalidwe

Chomaliza, inu ndi okondedwa wanu muyenera kusamalira ana anu kuti akule m'chikhalidwe. Kunyumba kwa banja lanu kukhale danga labwino kwa ana kuti akule muchikhalidwe chao ndi anthu. Muyenera kuwaphunzitsa kuti azindikire pakati pa zabwino ndi zoipa. Muyeneranso kuwaphunzitsa iwo m'mene angayanjanire ndi anzao m'mabwalo osiyanasiyana a wanthu.

ZOFUNIKIRA ZOYAMBIRIRA KWA MKAZI WAKE

Baibulo likuyankhula poyera zokhudza udindo wa mwamuna kwa mkazi wake. Maundindo amenewa ndiwoyeneranso Mbusa wa Chipentekoste. Ngati munthu wa umulungu, udindo wako kwa mkazi zikuphatikizapo zinthu izi:

Kuwonetsera Chikondi

Paulo analemba kuti mwamuna ayenera kuti "Akonde mkazi wake, monganso Khristu anakonda Mpingo" (Aefeso 5:25). Chikondi cha Khristu pa Mpingo, chinali cha msembe komanso chosadzikonda. Chikondi chanu pa mkazi wanu chikhale chomwecho. Lengezani chikondi chanu powonekera komanso pobisika.

Pamene muli nokha ndi iye, nthawi zonse mudziti“Ndimakukonda.” Pamene muli powonekera, muyenera kuwonetsera chikondi chanu pa mkazi wanu. Mwachitsanzo, mutha kulengeza ku mpingo, “Ndine wodalitsika kukhala limodzi ndi mkazi wanga lerolino. Ndi mkazi wodabwitsa kwambiri komanso wabwino kwa ana athu. Ndimamukonda kwambiri.”

Machitidwe amenewa ndi ena ambiri ofanana athandizira kumangilirana kwa mkazi wanu komanso ku mpingo. Muyeneranso kuwonetsera chikondi kwa mkazi wanu kudzera m’machitidwe anu. Ndiko kuti, kumuyankhula modekha, kukonda iye koyambirira, ndi kumuthandizira pa ntchito zake.

Kupereka Chithandizo

Udindo wachiwiri womwe inu ngati Mbusa wa Chipentekoste mulinawo pa mkazi wanu ndi ana anu ndiko kuwapatsa iwo thandizo ndi kuwaganizira. Petro analembera amuna, “Khalani nao [akazi] monga mwa chidziwitso, ndi kuchitira mkazi ulemu” (1 Petro 3:7).

Monga mwamuna wa Chikhristu, muyenera kuti muthandize mkazi ndi ana anu ndi zinthu zakuthupi pakupereka kwa iwo zinthu zokwanila ngati, pogona, chakudya, ndi zovala. Ngakhale kuti mkazi wanu ndi ana ena akuluakulu atha kuthandizirapo mdera limeneli, inu ngati mwamuna m’nyumbamo, muli oyambirira kusenza udindo umenewu.

Njira ina yomwe mutha kuthandizira mkazi wanu ndi kumuthandizira kukwaniritsa maitanidwe ake mu utumiki. Chonena chanu mudziti, “Ngati sindingathe kuthandizira mkazi wanga kufikira zolinga zake, ndithandizira bwanji mpingo kuchita zomwezi?” kuti muchite izi, muyenera kuzindikira momasuka kuti Mulungu ali ndi maitanidwe pamoyo wa mkazi wanu, monga mmene Iye ali ndi maitanidwe pa moyo wanu. Muyenera tsono kuyenda naye mmapemphero ndi uphungu, kumuthandizira kuti azindikire ndi kutsatira cholinga cha Mulungu pa moyo wake.

Kupereka Chitetezo

Udindo wachitatu omwe muli nawo pa mkazi wanu ndiko kumuteteza iye kuzolimbana naye zakuthupi, zomvaimva, ndi za uzimu. Pa mlingo wodziwikiratu, umuthandizire iye kuthupi. Baibulo limatcha mkazi “Chotengera chochepa mphamvu” mu chiyanjano cha ukwati (1 Petro 3:7). Ngati bwenzi lamphamvu kuthupi, muyenera kuyima molondera nthawi zonse, wokonzekeratu

kuteteza iye kuchokera ku zolimbana ndi iye. Kudziwa izi kumpangitsa iye kumva kutetezedwa ndi kulemekezedwa.

Mopitilira, muyenera kuteteza mkazi wanu ku zomvaimva zomuwononga. Mwatsoka, mkazi wa mbusa nthawi zambiriamakonda kunenedwa. Azipongozi ndi mamembala akuthupi nthawi zambiri amamunena iye ndi ana ake. Ena amalephera kuonetsera kuyamika kwao pa zomwe iye amachita. Izi zitha kukhala zopweteka kwambiri kwa iye. Muyenera kudziwa m'mchitidwe uwu mu mpingo, ndipo muyenera kuthandiza mkazi wanu ndikupereka thandizo lofunikira m'maimvaimva ake.

Chotsirizira, popeza mkazi wa mbusa ndi mdani woyamba wa Satana, muyenera kumuteteza iye mu uzimu. Mutha kupanga izi pakum'mangira mpanda wa pemphero mozungulira iye. Komanso, pamene pafunika, muyenera kuima popasuka pakati pa iye ndi mdani (Ezekiele 22:30).

KUFUNIKIRA KWAMBIRI KWA ANA AKE

Mbusa wa Chipentekoste ayeneranso kuona ana ake kukhala ofunikira. Chotsatira ku udindo wakukonda ndi kusamala mkazi wake, ndikuti ali ndi udindo wakukonda ndi kusamalira ana ake. Ayenera kusamalira iwo monga Atate wake akumwamba asamalira iye. Ayenera ku "Awalere iwo m'maleredwe ndi chilangizo cha Ambuye" (Aefeso 6:4).

Monga munthu wa umulungu komanso tate wachikhristu, muli ndi maudindo atatu ofunikira kwa ana anu:

Khalani Chitsanzo cha Chikondi Cha Mulungu

Choyamba, mukhale chitsanzo cha chikondi cha Mulungu kwa ana anu. Ana amaumba malingaliro ambiri okhudza Mulungu pakuona atate wao. Ngati tate wao wakudziko lapansi ndi okoma mtima ndi okonda, amaonanso kuti Tate wao wakumwamba ngati okoma mtima ndi okonda. Ngati tate wao wakudziko lapansi ndi wankhanza, anao amaona Mulungu munjira yomweyo. Pamene mukuonetsera zikhalidwe zaumulungu, ngati chikondi, kulemekeza, kutumikira, ndi kudalira, ana anunso adzitha kulandira malangizo ndi kukonzedwa mnyumbamo. Baibulo lafotokoza chikhalidwe chenicheni cha chikondi:

> "Chikondi chikhala chilezere, chili chokoma mtima; chikondi sichidukidwa; chikondi sichidziwa kudzitamanda, sichidzikuza, sichichita zosayenera, sichitsata za mwini yekha, sichipsa mtima sichilingilira zoipa; sichikondwera ndi chinyengo, koma chikondwera ndi choonadi; chikwirira zinthu zonse, chikulupirira zinthu zonse, chiyembekeza zinthu zonse, chipirira zinthu zonse. Chikondi sichitha nthawi zonse." (1 Akorinto 13:4-8)

Uwu ndi mtundu wa chikondi omwe muyenera kuonetsera ana anu.

Atsogolereni Kwa Khristu

Kuphatikiza ku kuwaonetsera chikondi cha Mulungu, muyenera kuwatsogolera ana anu mu ubale wa iwo ndi Yesu Khristu. Nthawi yabwino yopangira izi ndi mkatikati mwa kupembedza pa banja panu. Mnthawi yakupembedzai, mutha kuonetsera dongosolo lachipulumutso kwa ana anu. Kenako, pamene nthawi ili yoyenera, mutha kupemphera ndi iwo kuti alandire Khristu kukhala mpulumutsi wao. Zikatha izi, zizakhala zofunikira kuti ana azalengeze poyera kudzipereka kwao kwa Khristu kudzera mu umboni ndi ubatizo wa m'madzi. Mudziyang'ananso danga loti muwatsogolere ana anu mu ubatizo ndi Mzimu Woyera. Kenako muthenso kuwalimbikitsa iwo kugawana chikhulupiriro chao ndi anzao.

Ongolerani Chikhalidwe Chao

Muyenera kukhala ndi dongosolo lomveka bwino pa chakuwongolera chikhalidwe cha ana anu. Inu ndi mkazi wanu muyenera kuwaphunzitsa iwo cholondola kuchokera ku cholakwika komanso mmene "Angapewere maonekedwe onse a choipa" (1 Atesa. 5:22). Muphunzitsenso ana kuti akhale a ulemu, okoma mtima, ndi kulemekeza aulamuliro, pamodzi ndi kufunikira kwa kuona mtima ndinso kulimbika pa ntchito. Malangizo apite patali pakuwathandizira iwo kuti apambane m'moyo.

Mutha kuchita izi pakukhala chitsanzo cha moyo wachiyero mnyumba, komanso kukambirana moganiza bwino zokhudza chikhalidwe ndi ana anu. Pamene ana anu akuona inu makolo awo mukuchita chilungamo moona mtima, mwachidziwikire afuna kutsatira inu. Nthawi zina mufunikira kuti mwachikondi mudzudzule ana anu kuti muwasinthe kuwachotsa ku kupusa ndi machitidwe omwe atha kuwaononga (Miyambo 29:15).

KUTHANDIZA BANJA NDI ACHIBALE

Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuonetsanso kukonda banja ndi achibale akwawo komanso a kwa mkazi wake. Achibale amenewa akuphatikizapo makolo, achimwene, alongo, asuweni, ndinso ena. Paulo analemba, "Koma ngati wina sadzisungiratu mbumba yake ya iye yekha, makamaka iwo a m'banja lake, wakana chikhulupiriro iye, ndipo aipa koposa wosakhulupirira" (1 Timoteo 5:8).

Komabe, pali nthawi zina pamene zofuna za mbumba zitha kukhala zotsutsana ndi malembo. Mwachitsanzo, banja lanu litha kufuna kukakamiza zikhalidwe pa banja lanu ngati miyambo yamdulidwe kapena kutchula kwa dzina la mwana. Mu nthawi ngati izi, muyenera kuwakonda, koma mokhazikika, kukana zonenazi.

Njira ina yomwe akubanja atha kuika zokakamiza pa inu ndi banja lanu ndi kubwera ndikukhala mnyumba mwanu kwa nthawi yaitali. Zotsatila zake, amakhala choyamwa chuma, maganizo, ndi maimvaimva a banja lanu. Zokakamiza nthawi zambiri zimaikidwa pa mkazi wa Mbusa, atha kufinyika kufikira pothodwa. Mu nyengo ngati izi, ngati mutu wa banja tengani ulamuliro wa nyengoyo ndi kukhazikitsa malire athanzi.

Mukumbukire chilimbikitso cha Paulo kwa Timoteo, monga zalembedwa m'mwambamu, kuti munthu athe kusamalira mbumba yake, *"makamaka iwo a m'banja lake*"*."* Ngati mwamuna wa Chikhristu, udindo wako oyambirira suli kwa mbumba yako koma kwa mkazi ndi ana ako. Choncho ndizofunikira kukumbutsa m'bale wanu yemwe angakhumudwe nanu pa zomwe baibulo lalamula kuti "Mubwevuke kwa mbale yense wakuyenda dwakedwake, wotsatsata mwambo umene anaulandira kwa ife" (2 At. 3:6), ndi kuti "Ngati munthu safuna kugwira tchito, asadyenso" (v. 10).

M'malo momatsutsana ndi zofuna za mbumba yanu nthawi ndi nthawi, inu ndi mkazi wanu, musankhiretu mtundu wa thandizo omwe mupereke kwa iwo. Pakuchita izi, mufunikira kugwirizana pa zokutsogolerani, monga: ndindani asankhe kumbali zonse za banja kuti athandizidwe ndani? Ndi kuti ndi nthawi yochuluka bwanji thandizo likhale likuperekedwa?

Cholinga chachikulu kwa mbumba ya banja lanu ndiko kukhala mchere ndi kuunika kwa iwo. Ndizotheka ndithu kumvera chikhalidwe chakwanu kufikira kuti umakhala osagwira ntchito mu utumiki. Uyenera kufunitsitsa kupeza muyezo

wabwino pakati pa kuthandiza ndi kukana kuthandiza. Komabe, nthawi zonse, banja lako lifunitsitse kuchitira umboni ku anthu a mabanja ena.

Ngati mbusa wa Chipentekoste, Mulungu wakuitana iwe kuti utsogolere mpingo mkukwaniritsa ntchito ya Mulungu. Komabe, pakuchita izi, usanyalanyaze banja lako. Usafike ponena kuti, “Ndabweretsa otayika kwa Khristu; koma ndataya banja langa lomwe.”

~ Mutu 8 ~

Kufunikira Kwa Pemphero

Monga chinali chikhalidwe chake, Mose anatuluka kunka kuchihemacho kuti akapemphere. Nthawi zonse anthu akamamuona akuchita izi, amayimitsa zomwe amachita ndikumuona iye kufikira atalowa m'chihema. Pamene Mose anali mkati mwa m'chihema kupemphera, mtambo umadza ndikuima pakhomo la chihemacho. Pamene anthu onse anaona izi, anadzidzidwa ndi kudabwa, ndipo anthu onse analambira Mulungu. Onse analimbikitsika podziwa kuti mtsogoleri wao nthawi zambiri amayankhulana ndi Mulungu. M'chitidwe uwu wa Mose unakhudza mnyamata omthandizira, Yoswa. Iye nthawi zambiri amamutsatira Mose ku chihema, ndikukhalabe kanthawi m'chihemamo Mose atachoka. Iye amafunitsitsa kwambiri kuti akhale monga mphunzitsi wake (fanizilani Eksodo. 33:8-11).

Palibe chomwe chimalimbikitsa mpingo ngati mbusa wopemphera. Satana saopa mapepala athu ama digiri omwe timawapeza kudzera mmaphunziro. Iye sachitanso manthandikuchuluka kwa ndondomeko yazachuma yathu mu mpingo kapena zomanga zokongola zomwe tili nazo. Chomwe Satana amaopa ndi mapemphero athu. Iye ndi magulu ake a ziwanda amanjenjemera pamene anthu ake a Mulungu agwa pamaondo mupemphero lodzodzedwa ndi Mzimu komanso lodzara ndi chikhulupiriro. Ngati mbusa wa Chipentekoste angalephere kupambana mu chilichonse, iye ayenera kupambana mukupemphera.

MOYO WA PEMPHERO

Obweretsa kusintha wankulu, Martin Luther, tsiku lina anati, “Kukhala mKhristu popanda pemphero mkosatheka kuposa kukhala ndi moyo koma osapuma.” Zomwe zili zoona kwa Mkhristu mosakaikitsanso ndi zoona kwa mbusa wa Chipentekoste. Munthu sangathe kutumikira ngati mbusa weniweni wa Chipentekoste popanda moyo wodzipereka wa pemphero. Yesu adawuza ophunzira ake kuti “Ayenera iwo kupemphera nthawi zonse, osafooka mtima” (Luke 18:1).

Ngati mbusa wa Chipentekoste, mumutenge Yesu ngati chitsanzo chanu. Moyo wa Yesu ndi utumiki wake unali wodzala ndi pemphero. Luka akulemba kuti, “Iye anazemba, nanka m’mapululu, nakapemphera” (Luka 5:16). Panthawi ina, “Ndipo kunali masiku awa, Iye anatuluka nanka kuphiri kukapemphera kwa Mulungu” (6:12). Panthawi ina, Iye anatenga Petro ndi Yohane, ndi Yakobo “Nakwera phiri kukapemphera” (9:28). Ndipotu, Yesu amapemphera pa danga lililonse. Monga Yesu, kutsogolera anthu a Mulungu,uyenera kukhala mayi ndi bambo wapemphero nthawi ndi nthawi. Palibe angatumikire mu mphamvu ya Mzimu Woyera popanda chikhalidwe chopitirira mu pemphero.

Kudzera m’pemphero, umadzikonzekeretsa wekha pa utumiki. Pamene mudikira m’pemphero, mumayandikira chifupi ndi Mulungu (Yakobo 4:8, Heb 10:22). Kuphatikiza apo, umapeza mphamvu za uzimu zomwe zimafunikira kuti ukhale moyo chifukwa cha Khristu, ndi mphamvu zomwe zifunikira kuti uchite utumuki bwino lomwe (Yesaya 40:31; Masalmo 40:1-3).

Baibulo litilimbikitsa kuti, “Muyendeyende mwa Mzimu, ndipo musafitse chilakolako cha thupi” (Agalatiya 5:16). Kuti muchite izi mufunikira kukhala pa chiyanjano pafupipafupi ndi Mulungu. Chiyanjanochi chimatheka kudzera m’pemphero. Mu nyengo ya pemphero, Mzimu Woyera adzakuyankhulani ndi kukupatsani chilimbikitso ndi chitsogozo. Pemphero lodzodzedwa ndi Mzimu Woyera lidzakukonzekeretsani pa nkhondo za Uzimu (Aefeso 6:12, 18).

UTUMIKI WA PEMPHERO

Kuonjezera pakukuza moyo wa pemphero, ngati mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuwona pemphero ngati njira yotumikira ena. Pali njira zitatu zomwe utha kutumikira ena kudzera mpemphero:

Kutumikira Kudzera Mpemphero la Mseri

Choyamba, mutha kutumikira ena kudzera mpemphero la mseri. Yesu adalitcha mtundu wa pemphero uwu kuti pemphero lachinsinsi. Anaphunzitsa kuti, "Koma iwe popemphera, lowa m'chipinda chako, nutseke chitseko chako, nupemphere Atate wako ali m'tseri" (Mateyu 6:6). Kumeneko kosaonekako, utaye nthawi yako mkupempherera zosowa za ena. Pamene mupemphera mutha kupembedzera ndi kulimbika mtima, podziwa kuti Mulungu amaona ntchito yako ya chikondi ndipo Iye adzayakha mapemphero anu. Mu ndime yomweyo, Yesu adalonjeza, "Ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe." Nthawi yako mpemphero itha kutenga mitundu yosachepera itatu:

1. Pemphero lakudzikhuthura. Choyamba, muyenera kupemphera modzipereka. M'mau ena, muthere nthawi mpemphero pakusunthira chifupi ndi Mulungu. Machitidwe awa amalimbikitsa ubale wako ndi Mulungu. Pamene mupemphera mu Mzimu Woyera, chikhulupiriro chanu chiumbika, komanso musungidwa m'chikondi cha Mulungu (Yuda 20-21; fanizilani Aroma 5:5). Kuchokera ku ubale otere ndi Mulungu mudzakhala ndi kuthekera kokwaniritsa utumiki wanu.[1]

2. Pemphero lakupembedzera. Kenako, monga zanenedwa mwambamu, ngati mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutaya nthawi pamaso pa Mulungu kupembedzera kwa Iye chifukwa cha zosowa za ena-makamaka chifukwa cha zosowa za iwo akulumikizidwa ku mpingo wanu. Nthawi zonse Yesu amapempherera ophunzira ake (Yohane 17:9). Mwachitsanzo, anawapempherera kuti chikhulupiriro chawo chikhalebe cha mphamvu (Luka 22:32). Iye anapitirira kuwapempherera kuti Mulungu ateteze iwo (Yohane 17:11-12, 15), komanso kuti akhale ndi chimwemwe (v. 13). Iye adawapempherera nso chifukwa cha kupatulidwa kwao (vv. 17-19) komanso kuti akakhale amodzi (vv. 21-23).

Mu njira yomweyo, mtumwi Paulo anapitiriza kupempherera chifukwa cha anthu a Mulungu. Adalemba kwa ophunzira a ku Aroma, "Kosalekeza ndikumbukira inu, ndi kupempha masiku onse m'mapemphero anga" (Aroma 1:9-10). Iye adawauza Aefeso, "Sindileka kuyamika chifukwa cha inu, ndi kukumbukira inu m'mapemphero anga" (Aefeso 1:16; fanizilani Akolose 1:9).

[1] Pa zambiri zokhudza kuyandikira chifupi ndi Mulungu, onani mutu 15: "Chizolowezi Chodzipereka Champhamvuu."

Ngati abusa a Chipentekoste tiyenera kutsatira zitsanzo za Yesu ndi Paulo ndi kuthera nthawi yochuluka mpemphero, kupembedzera chifukwa cha ena.[2]

3. Kupemphera ndi Kusala kudya. Chotsiriza, ngati mbusa wa Chipentekoste, nthawi zambiri udzipemphera ndi kusala kudya. Mwambo wa uzimu wakusala kudya ndi kupemphera ukuthandizirani kubweretsa mzimu wanu kuchiyanjanitso ndi Mzimu wa Mulungu. Pamene mugwiritsa nthawi yanu mpemphero ndi kusala kudya, thupi lanu limafika pogonja, ndipo Mzimu wanu umakonzekeretsedwa momveka bwino kuti uthe kuzindikira liwu la Mzimu (fanizilani Agal. 5:16-17).

Kutumikira Kudzera Mkupempherera

Nthawi zambiri ngati mbusa wa Chipentekoste mudzayitanidwa kuti mukatumikire mpemphero kwa munthu-ku-munthu. Kutumikira kumeneku kumachitika pamene mupempherera wina amene ali ndinu. Mtundu wa pempherowu umachitika nthawi zambiri mkatikati mwa nthawi zakupemphera kutsogolo kwa mpingo. Kuthanso kuchitika kunyumba kapena kuchipatala munthawi yomwe akuyendera. Kapena ithanso kuchitika pamsika mnthawi yakufalitsa uthenga wabwino. Mapemphero awa amaphatikizapo nthawi zambiri kusanjika manja kapena kudzodza ndi mafuta (fanizilani Machitidwe 19:6; Yakobo 5:14). Nthawi zonse pemphero ili limachitidwa mu chikhulupiriro (Yakobo 5:15).

Zitsanzo zinayi za pemphero la munthu-ku-munthu ndi kupemphera ndi anthu kuti apulimutsidwe, kupemphera ndi anthu kuti achiritsidwe, kupemphera ndi anthu kuti amasulidwe kuchokera ku magoli a ziwanda, komanso kupemphera ndi anthu kuti adzazidwe ndi Mzimu Woyera. Uyenera kukhala wodziwa kachitidwe ka izi mu utumiki. Mu nyengo iliyonse, muyenera kuonetsera kulimbika mtima kwanu pa mau a Mulungu, kuyankhula mau a chikhulupiriro ndi chilimbikitso, komanso kuonetsera moona mtima kukhudzidwa kwanu ndi munthu amene mukumpempherera.[3]

---

[3] Pa zambiri zokhudza kupempherera anthu, onani, mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu"; ndi mutu 22: "Kumenya Nkhondo za Uzimu." Komanso, onani buku lotchedwa, *Utumiki Wamphamvu: Kutumikira mu Mphamvu ndi Kudzoza kwa Mzimu Woyera,* la Denzil R. Miller, lomwe limapereka uphungu othandiza mkupempherera anthu kuti achiritsidwe, kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndikumasulidwa ku magoli a ziwanda. Litha kutengedwa pa webusaiti ya DecadeofPentecost.org.

Kutumikira Kudzera M'mapemphero a Pagulu

Munthawi zina mudzaitanidwa kuti mupemphere mapemphero a pagulu. Abusa ena amapereka mapemphero a ubusa pa mpingo wao m'mawa wa la Mulungu lililonse. Kuphatikiza apo, mbusa wa Chipentekoste nthawi zambiri amaitanidwa kuti apemphere pa mkumano wa magulu monga, maliro ndi ukwati. Pamene mwafunsidwa kuti mupemphere mu zochitika ngati izi, muyenera kupemphera ndi ulemu komanso chisomo. Pemphero lanu la pagulu lisaperekedwe ngati chionetsero kapena mwambo chabe. Nthawi zonse muyenera kupemphera moona mtima. Yesu adachenjeza, "Ndipo pamene mupemphera musakhale ngati onyengawo; chifukwa iwo akonda kuimirira ndi kupemphera m'masunagoge, ndi pa mphambano za makwalala, kuti aonekere kwa anthu" (Mateyu 6:5).

KUTSOGOLERA MPINGO M'PEMPHERO

Mbusa wa Chipentekoste sakungoyenera kukuza moyo wake okha wa pemphero, ayeneranso kuumba utumiki wa mphamvu wa pemphero mu mpingo omwe akutumikira.

Kulalikira ndi Kuphunzitsa za Pemphero

Chifungulo chimodzi chofunika mukukuza utumiki wapemphero wa mphamvu mu mpingo ndi kulalikira ndi kuphunzitsa nthawi zambiri pa mutuwu. Pakuchita izi, mudzakhala mukutsatira chitsanzo cha Yesu, amene mwa Iye mwini anaphunzitsa zambiri pa zokhudza pemphero (Luka 18:1; Mateyu 6:5-15).

Muntha kulimbikitsa Akhristu kupemphera pakuwagawira maumboni a mmene Mulungu wayankhila mapemphero anu mbuyomu. Maumboniwa atha kuchokera m'baibulo, mu mbiri, kapena zomwe zikungochitika mnyengo imeneyo. Muyeneranso kutenga nthawi kuphunzitsa ziphunzitso zokhudza ubwino ndi kachitidwe ka pemphero.[4]

[4] Mndandanda wa Kulalikira ndi kuphunzitsa za pemphero zitha kupezeka mu buku, *Kupembedzera Maiko: Ndondomeko zama Ulaliki 100 a Pemphero la Utumwi,* lomwe litha kutengedwa mwa ulere pa tsamba la www.DecadeofPentecost.org.

Kukhala Chitsanzo M'pemphero

Osamangophunzitsa kokha zokhudza pemphero, muyenera kuwaonetsa okhulupirira m'mene angapemphelere. Umu ndi m'mene Yesu anaphunzitsira ophunzira ake. Iye sanangowaphunzitsa za pemphero, koma anawaonetsanso ndi moyo wake. Iye adaonetsa chitsanzo cha moyo wa pemphero pamaso pao. Ophunzira a Yesu anazindikira m'mene iye anayendera mchiyanjano ndi Atate wake wakumwamba mosasintha. Nthawi ina, atatha kumuona Iye mkupemphera, adamfunsa Iye, "Ambuye, tiphunzitseni kupemphera monganso Yohane anaphunzitsira ophunzira ake" (Luka 11:1). Ngati mbusa wa Chipentekoste, uyenera kukhala moyo wapemphero onga otere kufikira mamembala ako adzakufunse, "Abusa tiphunzitseni kupemphera monganso Yesu anaphunzitsira ophunzira ake."

Kukonzekera chifukwa Cha Mapemphero

Mbusa wa Chipentekoste ayenera kukonzekeretsa mpingo ku pemphero. Mutha kuchita izi pakukonza magulu a mapemphero komanso kukonza dongosolo la zochita za mapemphero, monga zotsatilazi:

Kukonza magulu amapemphero. Mukuyenera kuti mulimbikitse kukonza kwa magulu apaderadera amapemphero mu mpingo. Magulu amenewa atha kukonzedwa ngati othandizira ma utumiki ngati utumiki wa abambo, utumiki wa amayi, utumiki wa achinyamata, ndi ena. Atha kupangidwanso kuti athane ndi chosoweka china mu mpingo, kudera, kudziko, kapena dziko lonse. Zosoweka izi zitha kukhala maubale kapena uzimu, dera kapena kuzungulira dziko lonse. Mwachitsanzo, mamembala ena atha kufuna kupemphelera chitsitsimutso mu mpingo, pamene ena atha kufuna kupemphelera mtendere mu dziko. Zinthu zambiri zosoweka zitha kuzindikirika zomwe zifunikira pemphero.

Kukonza dongosolo la zochitika za mapemphero. Muthanso kufuna kuphatikiza zochitika za mapemphero mu kalendala ya zochitika za mpingo. Muyenera, ndithu, kuyika dongosolo lopitirira la mikumano ya mapemphero pa mpingo, monga mapemphero a pakati pa Sabata. Mufunikiranso kuyika dongosolo la zochitika zapadera zamapemphero monga mapemphero ochitikira malo ena kapena masabata a mapemphero apaderadera.

Mwachitsanzo, mbusa wina wa Chipentekoste anayika sabata limodzi la mapemphero akathithi ndi kusala kudya kawiri m'chaka chilichonse mu mwezi wa Januwale komanso Julaye. Mu kukonzekera zochitikazi, analimbikitsa ma

membala ake kuti asonkhanitse zopembedzera kuchokera kwa akubanja kwao, anzao, achifupi nao, ndi ogwira nao ntchito. Kenako amalembo zopembedzerazi pa mapepala omwe anakonza ndikuwagawa kwa mamembala kuti apemphere nthawi za mkumano wa mapemphero a mmawa ndi madzulo. Madalitso akuluakulu anabwera ku mpingowu ndi dera lonse kudzera ku zochitikazi.

Abusa ambiri a Chipentekoste amayika dongosolo la ndandanda wa mikumano ya mapemphero kulunjika lamulungu la Pentekoste chaka chilichonse. (Lamulungu la Pentekoste limadza nthawi zonse masabata asanu ndi awiri pakatha lamulungu lapasaka.)M'mikumano ya paderayi okhulupirira amayitanira pa Mulungu kuti atsanule Mzimu Woyera pa mpingo. Iwo amapempheranso kuti mu nyengo yakukondwelera PENTEKOSTE Akhristu ambiri apatsidwe mphamvu ndi Mzimu Woyera (Machitidwe 1:8; 2:4). Komanso amapemphera kuti anthu ambiri abwere kwa Ambuye monga zinachitikira patsiku loyamba la Pentekoste (2:41).

Muthanso kufuna kuti muyike mndandanda wa mapemphero apachaka ndi ogwira ntchito apa mpingo komanso atsogoleri. Muyenera kufunitsitsa chitsogozo cha Mulungu mwakhama molingana kuti mudziwe chomwe mutsindike mu mndandanda wa mapemphero omwe muyike pa mpingo.

Kupempherera Ntchito ya Mulungu

Ichi ndichopemphelera chimodzi chofunika kuti chidzipezeka mu mpingo uliwonse wa Chipentekoste mu Afirika. Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuonetsetsa kuti mpingo wake ukupemphelera mowilikiza chifukwa cha kukula kwa ntchito ya Mulungu mu dziko lapansi. Ichi chinali chopembedzera cha Yesu, ndipo chisanyalanyazidwe (Mateyu 9:37-38). Muyenera tsono kutsogolera mpingo wanu mu pemphero lodzipereka chifukwa cha kupita patsogolo kwa ufumu wa Mulungu mu dera, dziko, m'zigawo za maiko komanso dziko lonse lapansi. Muyenera kutsogolera iwo mu mapemphero chifukwa cha atumwi otumizidwa ndi mpingo wonse, komanso iwo othandizidwa ndi mpingo wanu. Ndipo pempherani nthawi zonse chifukwa anthu zikwizikwi am'magulu a wanthu omwe sanafikiridwe m'dziko lapansi.[5]

[5] Uthenga okhudza magulu a anthu omwe sanafikiridwe ndi uthenga wabwino utha kupezeka pa webusaiti ya www.JoshuaProject.net.

KUTSOGOLERA MKUMANO WA MAPEMPHERO

Mbusa wa Chipentekoste ayenera kudziwa mmene angathe kuchitira mapemphero mwa bwino lomwe. Apa pali zina mwa zokutsogolerani zothandizira kutsogolera mkumano wa mapemphero.

Konzekeranitu

Monga mmene m'machitira ndi chochitika chofunikira chilichonse mu mpingo, muyenera kukonzekeratu ku mkumano wabwino wamapemphero. Muyenera kusankha nthawi ndi malo ochitira kumanowo. Koposa mufunikira kudziwiratu cholinga cha mapemphero komanso kuti m'chiyani chomwe mapemphero akutsindika. Ndipo muyenera kupanga mndandanda wa zopemphelera zomwe zikafikiridwe mu mkumanowo. Muthanso kufuna kuti mupeze zambiri zoyenera zokhudza zomwe mukukapemphelera. Kenako mudzagawana zomwe mwadziwazi ndi otenga mbali pa nthawi yoyenera mu mkumano wamapemphero.

Sungani nthawi— Khalani achindunji

Pamene mutsogolera mkumano wa mapemphero, mufunikira kusunga nthawi ndi kukhala achindunji. Munjira ina, muyenera kuyamba ndi kumaliza mkumano wa mapemphero pa nthawi yoyikidwa. Anthu ena ndi otanganidwa, ndipo adzathokoza mmene mulemekezere nthawi yao. Zotsatila zake, iwo adzafunanso kuti apezeke mmapemphero ena.

Koposa, pamene mutsogolera mkumano wamapemphero,muyenera kukhala achindunji. Izi zikutanthauza kuti musaloremkumano wamapemphero kukhala wobalalika, koma mukhale pa chindunji. Kutumikira kochepa ndi kanthawi koyimba kochepa ndi zoyenera pamayambiriro a mkumano wamapemphero. Nthawi yochuluka ya mkumanowo ikhazikike pakupemphera.

Khalani Otseguka kwa Mzimu Wa Mulungu

Ngakhale mkumano wamapemphero uyenera kukhala wa dongosolo ndi wachindunji, mtsogoleri wa mkumanowo akhale wotseguka ku mayendedwe a Mzimu Woyera. Iye alimbikitse anthu kupemphera mu Mzimu (Aroma 8:26-27; 1 Akorinto 14:15: Aefeso 6:18) ndi kukhalabe otseguka ku chitsogozo ndi kuonekera kwa mphatso za uzimu (1 Akorinto 14:26).

MAONEKEDWE A MKUMANO WA MAPEMPHERO

Wina atha kufunsa, "Kodi mkumano wa mapemphero a Chipentekoste umaoneka bwanji?" Yankho la mfunsoli likupezeka M'baibulo. Buku la Machitidwe likutipatsa ife chitsanzo cha mkumano wa mapemphero mu mpingo woyamba. Mkumano wamapemphero unachitika patangotha Tsiku la PENTEKOSTE.

Mpingo umadutsa mu chizunzo chachikulu. Atsogoleri Achiyuda adagwira Petro ndi Yohane. Adawaopseza iwo ndikuwauza kuti asiye kulalikira mu dzina la Yesu. Pamene iwo adawamasula atumwi awiriwo, anabwerera ku mpingo ndikufotokozera zomwe zinawachitikira. Akhristu anayamba kupemphera. Pemphero lao ndi zotsatira za pemphero zinalembedwa mu Machitidwe 4:23-31. Kuchokera mu mkumano wamapempherowu, tikuphunzirapo zinthu zitatu zofunikira zokhudza mmene tingachitire mkumano wamapemphero lero lino:

Mmene Tingamapempherere

Choyamba, tikuphunzira khalidwe lakapempheredwe, *kapena mmene tingapempherere*. Baibulo limanena za Akhristuoyambirirawo kuti, "Anakweza mau kwa Mulungu ndi mtima umodzi" (Mach. 4:24). Kupemphera kwao kunali kwakulu ("anakweza mau") ndipo kunali kwa umodzi ("anakweza mau ndi mtima umodzi"). Tikabwera pamodzi kupemphera, ifenso tifune Mulungu kwakulu, komanso tipemphere ndi mtima umodzi. Kuphatikiza apo mapemphero athu aperekedwe mwa chikhulupiriro (Marko 11:24). Iwo amene adapemphera tsiku limenero ku Yerusalemu adali ndi chiyembekezo chonse kuti Mulungu amva ndi kuyankha mapemphero ao.

Zomwe Zili M'mapemphero Athu

Chachiwiri, tikuphunzira zomwe zili mkati mwa mapemphero athu, *kapena zomwe tiyenera kuzipemphelera.* Akhristu oyambawo sadalunjika mapemphero ao pa mavuto ao, ngakhale kuti adalinawo ambiri. Iwo mmalo mwake adalunjika chidwi chao pa mphamvu ndi ukulu wa Mulungu (Mach. 4:24-25). Ndipo adapemphera kuti chifuniro cha Mulungu chichite (vv. 26-28). Koposanso iwo adafunsa Mulungu kuti awapatse kulimbika mtima kuti alakhule mau a uthenga wabwino, ngakhale mkatimkati mwa chizunzo (vv. 29-30). Pakufunsa Mulungu kuti "Kutambasula dzanja Lake," amafunsa Iye kuti ayende mwa mphamvu mwa

Mzimu wake (fanizilani Ezekiele. 37:1; Luka 11:20 ndi Mateyu. 12:28; Machitidwe 11:21).

Zotsatira za Mapemphero Athu

Chotsirizira, tikuphunzira za zomwe tingayembekeze kuti zichitika pamene tikupemphera. Ngati tingapemphere monga okhulupirira oyambawo, ifenso titha kuyembekeza Mulungu kuti apange kupezeka kwake kudziwike m'mikumano ya mapemphero athu. Baibulo, limati, "Ndipo m'mene adapemphera iwo, panagwedezeka pamalo pamene anasonkhanirapo; ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula mau a Mulungu molimbika mtima" (Machitidwe 4:31). Ngati tingapemphere monga adachitira, titha kuyembekeza Mulungu kuti ayankhe mapemphero athu munjira yomweyo adayankhira iwo. Titha kuyembekeza Iye kuti atidzaze ndi Mzimu Woyera ndikutipatsa mphamvu monga mboni za Khristu kwa otayika.

~ Gawo 3 ~

ZIKHULUPIRIRO ZA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

~ Mutu 9 ~

Amakhulupirira Baibulo

Pakhoma lakutsogolo la nyumba ya likulu la Africa's Hope ku Springfield, Missouri, USA, kuli mapu akulu a Afirika. Pamapupa pali chithunzi cha munthu wa ku Afirika atatambasula dzanja lake patsogolo pake. M'manja mwa munthuyo muli Baibulo. Iye akulalikira uthenga wabwino. Chifanizirochi chikuimira zikwi za alaliki a CHIPENTEKOSTE mu Afirika onse amene amalalikira Mau a Mulungu mokhulupirika kwa onse amene angamve. Zimayimiranso ubale wapadera wa Mbusa wa Chipentekoste ku Baibulo lake.

Baibulo silifanana ndi buku lina lililonse padziko lapansi.Ngakhale kuti limafotokoza mbiri yakale molondola, si buku la mbiri yakale chabe. Ngakhale kuti limaphunzitsa makhalidwe abwino, liri loposa buku la makhalidwe abwino. Anthu anzeru amachita chidwi ndi kuya kwa malingaliro ake, komabe Baibulo ndi loposa buku la nzeru. Baibulo liri ndi "mau enieni a Mulungu" (Aroma 3:2). Limavumbula mkhalidwe wauchimo wa anthu, ndipo limasonyeza njira ya chipulumutso kupyolera mwa Khristu. Mutu uwu uwonetsa ubale wapadera wa mbusa wa Chipentekoste ku Baibulo monga Mau a Mulungu.

MOMWE MBUSA WA CHIPENTEKOSTE AMALIONERA BAIBULO

Abusa a Chipentekoste amalemekeza kwambiri Baibulo. Iwo amakhulupirira kuti ndi uthenga wa Mulungu wopita kwa anthu—Mau amuyaya a Mulungu. Kwa

abusa a Chipentekoste, Baibulo limakhala ngati maziko a utumiki ndi machitidwe onse. Gawo 1 la "Zikhulupiriro za Chiyanjano cha Mpingo wa Assemblies of God pa dziko lonse," pamutu wa "Kuuziridwa kwa Malembo," likufotokoza mwachidule kaonedwe ka m'Baibulo ka Mbusa wa Chipentekoste kuti: "Malembo, Chipangano Chakale ndi Chatsopano, ndi ouziridwa ndi Mulungu ndipo ali vumbulutso la Mulungu kwa munthu aliyense, lamulo losalephera, amphamvu ndi ulamuliro pa chikhulupiriro ndi chikhalidwe (2 Tim. 3:15-17; 1 Ate. 2:13; 2 Pet. 1:21).[1] Kuti timvetse bwino tanthauzo la mauwa, tiyeni tigawe m'magawo ake anayi:

Mau Ouziridwa

Choyamba, mbusa wa Chipentekoste amakhulupirira kuti "Malembo, Chipangano Chakale ndi Chatsopano onse ndi mau ouziridwa ndi Mulungu." Tikamanena kuti Malembo *anauziridwa ndi Mulungu*, tikutanthauza kuti Mulungu mwa mphamvu zake zonse anasuntha paaneneri ndi atumwi akale, kuwatsogolera mwa uzimu kuti alembe maganizo ndi malingaliro amene Iye anasankha. Paulo anatsimikizira mfundo imeneyi pamene analemba kuti: "Lemba lililonse adaliuzira Mulungu" (2 Tim. 3:16). Petro analongosola mwatsatanetsatane mchitidwe wauzimu umenewu: "ndi kudziwa ichi poyamba, kuti palibe chinenero cha lembo chitanthauzidwa pa chokha, pakuti kale lonse chinenero sichinadze ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula" (2 Pet. 1:20-21).

Tikamanena kuti Baibulo *linauziridwa* ndi Mulungu m'mau, timatanthauza kuti kuuziridwa kwaumulungu kumafikira ku mau enieniwo a lembalo. Mulungu sanangouzira maganizo a m'Malembo, koma ankayang'anira ntchitoyo, kusankha mau omwewo mmene maganizo amenewa anasonyezedwera. Yesu anatsimikizira mfundo imeneyi pamene ananena kuti: "Nkwapafupi, koma kuti kalembo kakang'ono kachilamulo kagwe nkwapatali" (Luka 16:17). Kuuziridwa kukutanthauza kuti mau aliwonse m'Malembo ndi ouziridwa ndi Mzimu Woyera. Mauwo alipo chifukwa Mulungu anafuna kuti akhale pamenepo.

[1] Onani Zowonjezera 1: "Chiganizo cha Chikhulupiriro cha Chiyanjano cha Mpingo wa Assemblies of God pa dziko lonse."

Chifukwa chakuti Baibulo ndi louziridwa, moyenerera limatchedwa Mau a Mulungu. M'chenicheni, Baibulo limadzitcha ilo lokha kukhala "Mau a Mulungu" kapena "Mau a Yehova" nthawi zoposa makumi anayi.

Vumbulutso la Mulungu

Mbusa wa Chipentekoste amakhulupiriranso kuti Baibulo ndi "vumbulutso la Mulungu kwa munthu." Izi zikutanthauza kuti Mulungu waulula chifuniro chake kwa anthu kudzera m'mau a m'Malembo. Iye anauzira Baibulo kuti anthu amudziwe Iye, ntchito Zake, ndi njira Zake. Mwa kutipatsa Baibulo, Mulungu wasonyeza kuti ndi Mulungu wodziulula. Baibulo ndi umboni wakuti Mulungu amafuna kuti amuna ndi akazi onse kulikonse amudziwe Iye ndi dongosolo lake la chipulumutso.

Osalephera

Komanso, mbusa wa Chipentekoste amakhulupirira kuti Baibulo sililakwitsa. Kunena kuti Baibulo ndi losalakwa ndi kunena kutisilinalakwitsa chilichonse. Popeza kuti mau a m'Malembo anauziridwa ndi Mulungu, mfundo zake n'zoona ndipo zimene limanena n'zolondola. Wamasalimo ananena kuti, "Mau a Yehova ngoyengeka" (Masalimo 18:30) Yesu anatsimikizira mfundo imeneyi pamene ananena kuti: "Thambo ndi dziko lapansi zidzachoka, koma mau anga sadzachoka ai" (Mat. 24:35).

Ndikofunika kuti mbusa wa Chpentekoste amvetsetse kuti tikamanena kuti Baibulo ndi losalakwitsa, sitikunena za kumasulira kulikonse kwa Baibulo. Tikunena za Malembo monga momwe adawonekera mu zolembedwa zake zoyambirira. Omasulira Baibulo amayesetsa kumasulira molondola mauwo. Komabe, chifukwa chakuti iwo ndi anthu, n'zosapeweka kuti zolakwa zimachitika. Zolakwa izi, komabe, ndi zazing'ono. Masiku ano, tingakhale otsimikiza kuti Mabaibulo athu amafotokoza molondola mau a Mulungu monga mmene anaululira kwa olemba oyambirira.

Ulamuliro wa Mphamvu pa Chikhulupiriro ndi Chikhalidwe

Potsirizira pake, mbusa wa Chipentekoste amakhulupirira kuti Baibulo ndilo "ulamuliro wa mphamvu pa chikhulupiriro ndi chikhalidwe" cha wokhulupirira. Baibulo limauza mwamuna kapena mkazi wa Mulungu zimene ayenera kukhulupirira ndi mmene ayenera kukhalira. Chifukwa chakuti Baibulo ndi Mau

a Mulungu, lili lodalirika. Izi zikutanthauza kuti ziphunzitso zake ziyenera-kukhulupiriridwa, ndipo malamulo ake ayenera kutsatiridwa. Mfumu Davide anamvetsa mfundo imeneyi. Anatcha Mau a Mulungu "nyali ya kumapazi kwanga ndi kuwunika kwa panjira panga" (Mas. 119:105).

MMENE MBUSA WA CHPENTEKOSTE AMALIONERA BAIBULO

Kodi mbusa wa Chipentekoste ayenera kuliona bwanji Baibulo? Kodi ayenera kukhala ndi maganizo ndi malingaliro otani okhudza Malembo? Pokhulupirira kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu, mbusa wa Chipentekoste ayenera kuyandikira Baibulo ndi makhalidwe atatu:

Kulemekeza Koyera

Chifukwa chakuti mau a m'Malembo amachokera mumtima wa Mulungu woyera, Baibulo lenilenilo ndi loyera. Ndipo chifukwa chakuti Baibulo ndi lopatulika, mbusa wa Chipentekoste ayenera kulilemekeza kwambiri. Ayenera kulemekeza Mau a Mulungu ndi kuwachitira ulemu wopatulika. Paulo anayamikira Akhristu aku Atesalonika chifukwa cha mkhalidwe woterowo: "Pakulandira mau a Uthenga wa Mulungu, simunawalandire monga mau a anthu, koma monga momwe ali ndithu, mau a Mulungu, amenenso achita mwa inu okhulupirira" (1 At. 2:13). Chifukwa chakuti mbusa wa Chipentekoste amalemekeza Baibulo monga mau enieni a Mulungu, iye adzapewa kupotoza ziphunzitso zake n'cholinga chofuna kulichititsa kunena zimene iwo akufuna kuti linene. Petro akuchenjeza kuti amene amachita zimenezi "ndikudziwononga nao eni" (2 Pet. 3:16).

Chikondi Chozama

Sikuti mbusa wa Chipentekoste ayenera kulemekeza Baibulo kokha, ayenera kukhalanso ndi chikondi chenicheni paziphunzitso zake. Wolemba Masalimo 119 anasonyeza chikondi choterocho pa Mau a Mulungu. Pokhala ndi ndime 176, Salimo limeneli ndilo mutu wautali kwambiri m'Baibulo. Mutu umenewu ndi pemphero lalitali kwa Mulungu.

M'pemphero lochititsa chidwi limeneli, wolemba akufotokoza mobwerezabwereza chikondi chake pa Mau a Mulungu. Mwachitsanzo, amauza Mulungu kuti, "Ndipo ndidzadzikondweretsa nao malamulo anu, amene ndiwakonda" (v. 47). Iye amakumbutsanso Mulungu mmene mau Ake akhudzira

moyo wake. Iye anati: “Mtima wanga wasweka ndi kukhumba maweruzo anu nyengo zonse…. Mboni zanu zomwe ndizo zondikondwetsa ndizo zondipangira nzeru.” (vv. 20, 24). Mofanana ndi wa Masalimo, mbusa wa Chipentekoste ayenera kukulitsa chikondi chenicheni pa Mau a Mulungu.

Chidaliro Cholimba

Pokhala kuti mbusa wa Chipentekoste amakhulupiriradi kuti Baibulo ndi lowuziridwa ndi Mulungu, amayandikira kapenakulifikira ndi chidaliro cholimba. Amadziwa kuti angakhulupilire zilengezo ndi malonjezo ake. Chifukwa mbusa wa Chipentekoste amakhulupirira Baibulo kotheratu, monga Abrahamu, ali wotsimikiza kwanthunthu kuti zimene Mulungu walonjeza adzachita ndithu (Aroma 4:21).

Mbusa wa Chipentekoste sikuti amangokhulupirira kuti Baibulo ndi loona, iye amamvetsetsa kuti ndi lamphamvu. Kudzera m’Mau a Mulungu chilengedwe chinalengedwa (Yohane 1:1-3). Baibulo limanena kuti: “Mau a Mulungu ali amoyo ndi ochitachita. Ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse” (Aheb. 4:12). Paulo analongosola uthenga wabwino monga “mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa” (Aroma 1:16). Ndime zimenezi ndi zina zambiri zimanena za mphamvu ya Mau a Mulungu. Mwachitsanzo, polankhula kudzera mwa mneneri Yesaya, Mulungu ananena za Mau ake kuti: “Monga mvula imagwa pansi ndi matalala, kuchokera kumwamba yosabwerera komweko, koma ikhamiza nthaka ndi kuibalitsa, ndikuiphukitsa, ndi kuipatsitsa mbeu kwa wodzala, ndi chakudya kwa wakudya; momwemo adzakhala mau anga amene atuluka m’kamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine chabe, koma adzachita chimene ndifuna, ndipo adzakula m’mene ndinawatumizira (Yesaya 55:10-11).

Mowonjezera, Baibulo limatiuza kuti Mau a Mulungu amasonyeza njira (Mas. 119:105), amapulumutsa moyo (Yakobo. 1:21), amalenga chikhulupiriro (Aroma 10:17), amapereka moyo (1 Pet.1:23), amayeretsa (Yoh. 17:17), kumangirira (Mach. 20:32), kuchiritsa ndi kupulumutsa (Mas. 107:20), kuyeretsa (Yoh. 15:16), ndi zina zambiri. Chifukwa cha choonadi champhamvu chimenechi, mbusa wa Chipentekoste ali ndi chidaliro cholimba m’Mau a Mulungu.

UDINDO WA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE OKHUDZA BAIBULO

Monga mbusa wa Chipentekoste muli ndi maudindo ena pa Mau a Mulungu. Nazi zisanu ndi chimodzi mwa maudindo amenewo:

Kudziwa Baibulo

Choyamba, muyenera kukhala ndi chidziwitso chozama cha Malembo. Palibe chimene chimamuyenereza mbusa wa Chipentekoste kuti agwire ntchito choposa kudziwa bwino Baibulo. Ndipo palibe chomwe chimamulepheretsa iye kukhala woyenerera kuposa chidziwitso chozama, cham'mwamba cha Malembo.Chifukwa chake muyenera kudzipereka pakufuna kwa moyo wanu wonse kumvetsetsa Malembo. Mutha kuchita izi m'njira zitatu:

1. Kuwerenga tsiku ndi tsiku. Mungapeze chidziwitso cha Mau a Mulungu mwa kuwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku. Choncho muyenera kukulitsa mwambo wa kuwerenga Malembo.[2] Mukhoza kumaliza Baibulo m'chaka chimodzi mwa kuwerenga pafupifupi mphindi khumi ndi zisanu patsiku. Ngati mutsatira chizolowezi chimenechi, tsiku ndi tsiku, chidziŵitso chanu cha Baibulo chidzawonjezeka.

2. *Kuwerenga mwadongosolo.* Mukhoza kuwonjezera chidziwitso chanu cha Malembo posanthula Baibulo mwadongosolo. Baibulo limanena za mchitidwe umenewu pakati paokhulupirira Achiyuda ku Bereya. Limati: "Analandira mau[a uthenga wabwino] ndi kufunitsa kwa mtima onse, nasanthula m'malembo masiku onse, ngati zinthu zina zotero" (Mach. 17:11). Mungakhale wanzeru kutengera mchitidwe wa Abereya wosanthula mosamalitsa Mau a Mulungu.

Mudzayeneranso kupanga nkhokwe yamabuku yaumwini yokuthandizani kuphunzira Malembo. Nkhokwe imeneyi iyenera kukhala ndi mabuku ofotokoza za m'Baibulo monga ndondomeko ya malembo kapena mau m'buku, ndemanga yomasulira ndi yofotokozera mitu ndi ndime za m'Baibulo, ndi maphunziro ena a Baibulo. Iyeneranso kukhala ndi Baibulo lophunzirira bwino.Baibulo labwino

[2] Kuti mudziwe zambiri onani Mutu 15: "Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu."

kwambiri lophunzirira Chipentekoste ndi Baibulo la Moyo Wochuluka, lofalitsidwa ndi Life Publishers ku Springfield, Missouri, USA.[3]

Ngati n'kotheka, muyenera kumaliza maphunziro anu kusukulu ya Baibulo ya Chipentekoste. Izi zidzakulitsa chidziwitso chanu cha Malembo ndi luso lautumiki. Afirika Assemblies of God ili ndi dongosolo lalikulu la maphunziro autumiki m'dziko lonse la Afirika. Masukuluwa akuphatikizapo ogonera pompo komanso omwe wophunzira amangoyendera. Mutha kupeza sukulu ya Baibulo ya Assemblies of God pafupifupi m'maiko onse a kum'mwera kwa Sahara ku Afirika ndi maiko amu Afirika omwe ali kufupi ndi Nyanja yaikulu ya Indian. Sukulu zimenezi zimapereka maphunziro kwa atumiki omwe ndia Assemblies of God ndi iwo omwe si a Assemblies of God.[4]

3. Kuloweza pamtima. Muyeneranso kuloweza Malembo mwadongosolo. Cholinga chabwino ndi kuloweza lemba kapena ndime yatsopano pamlungu kapena sabata imodzi. Kuphatikiza apo, ndi chizolowezi chabwino kuloweza pamtima lemba lililonse kapena ndime ya Lemba yomwe muyenera kuphunzitsa kapena kulalikirako. Kuchita zimenezi kudzakuthandizani kukhala ndi ufulu wochuluka polalikira.Zidzawonjezeranso kwambiri ndime zoloweza pamtima.

Kutsatira Miyezo Yake

Chachiwiri, monga mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutsatira miyezo ya Baibulo. Sikokwanira kudziwa zimene Baibulo limaphunzitsa, muyenera kulora ziphunzitso zake kuwongolera moyo wanu ndi utumiki wanu. Baibulo limalimbikitsa kuti: "Khalani akuchita mau, osati akumva okha, ndikudzinyenga nokha" (Yakobo 1:22; onaninso Aroma 2:13). Pamodzi ndi wa Masalimo, muyenera kupemphera moona mtima, "Ndinasankha njira yokhulupirika; ndinaika maweruzo anu pamaso panga. Ndimamatika nazo mboni zanu; musandichititse manyazi, Yehova" (Mas. 119:30-31).

---

[3] Baibulo limeneli limatchedwanso kuti Baibulo la Moyo mu Mzimu. Limadziwikanso kuti "Baibulo la Moto," ndipo lafalitsidwa m'zinenero zoposa 60 padziko lonse. Kuti mudziwe zambiri, onani pa https://www.firebible.org/.

[4] Mndandanda wa masukulu a Baibulo a Assemblies of God mu Afirika ukupezeka pawebusaiti ya Africa Theological Training Service (ATTS): https://Africaatts.org/.

Kumasulira Mau a Choonadi Molondola

Chachitatu, monga mbusa wa Chipentekoste, muyenera kudzipereka kuti mumasulire bwino "mau a choonadi" (2 Tim. 2:15). Popeza mumakhulupirira kuti Baibulo ndi Mau amuyaya a Mulungu kwa anthu, muyenera kukana mayesero aliwonse opotoza Malembo mwadala kuti agwirizane ndi malingaliro anu. Mudzamvera chenjezo la Petro kwa “anthu osaphunzira ndi osakhazikika apotoza, monganso atero nao malembo ena, ndikudzionong a nao eni” (2 Pet. 3:16). Ndipo muyenera kumvera mosamalitsa lamulo la m’Malembo la “Koma iwe, lankhula zimene ziyenera chiphunzitso cholamitsa” (Tito 2:1).

Kupititsa patsogolo Ntchito Yake Mokhulupirika

Chachinayi, muyenera kudzipereka kuti mumvetsetse bwino lomwe ndikupititsa patsogolo mwachangu ntchito ya Mulungu monga yawululidwa m'Malembo. Baibulo limavumbula kuti Mulungu ndi Mulungu wautumwi ndipo akugwira ntchito yokwaniritsa ntchito yake padziko lapansi. Ntchito imeneyi nthawi zina imatchedwa *missio Dei*. Mulungu ali pa ntchito yake kuti awombole ndi kuitanira kwa iye yekha anthu ochokera ku mafuko onse, chiyankhulo chilichonse ndi mtundu uliwonse padziko lapansi (Chivumbulutso 5:9).[5]

Monga Mbusa weniweni wa Chipentekoste, muyenera kutsogolera mpingo wanu kuti mugwirizane ndi Mulungu mu utumiki uwu (Mateyu 24:14). Kuti muchite izi, muyenera kumvetsetsa bwino lomwe zomwe Baibulo limaphunzitsa ponena za ntchito ya Mulungu. Ndipo muyenera kudzipereka kuti mutsogolere mpingo wanu kuchita gawo lake pokwaniritsa cholingacho.

Kulalikira ndi Kuphunzitsa Mau

Chachisanu, ngati mbusa wa Chipentekoste, muyenera kulalikira mokhulupirika ndi kuphunzitsa Mau a Mulungu kwa anthu anu. Pochita zimenezi, mudzawathandiza “koma kulani m’chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu (2 Pet. 3:18). Ndipo mudzaonetsetsa kuti anthu a Mulungu “akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iliyonse yabwino”

[5]Kuti mudziwe zambiri za ntchito ya Mulungu, onani buku la Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Chiphunzitso cha M’baibulo cha Utumwi*, lolembedwa ndi Paul York

(2 Tim. 3:17). Ichi ndi chifukwa chimodzi chofunika kwambiri chimene Paulo analimbikitsira Timoteo, mwana wake m'chikhulupiriro, kuti: "Lalikira mau; chita nawo pa nthawi yake; popanda nthawi yake; tsutsa; dzudzula, chenjeza, ndi kuleza mtima konse ndi chiphunzitso" (2 Tim. 4:2).

Mbusa wa CHIPENTEKOSTE amene amaphunzitsa Mau a Mulungu mokhulupirika adzalandira mphotho (Mat. 24:45-47). Amene alephera ntchito imeneyi adzaweruzidwa koopsa (Yakobo 3:1).

Kuteteza Molimba Choonadi Chimene Baibulo Limaulula

Pomaliza, ngati mbusa weniweni wa Chipentekoste, muyenera kukhala okonzeka kuteteza chowonadi chowululidwa m'Malembo. Monga Paulo, muyenera kukhala "chokanira cha Uthenga Wabwino" (Afilipi 1:16). M'mau a mtumwiyo, "wogwira mau okhulupirika monga mwachiphunzitso, kuti akakhoze kuchenjeza m'chiphunzitso cholamitsa, ndi kutsutsa otsutsana naye." (Tito 1:9)

Poganizira izi, muyenera kuyang'anira nkhosa za Mulungu mwakhama kuti muteteze oyera mtima kwa aphunzitsi onyenga ndi ziphunzitso zabodza (Mach. 20:28-31). Mungachite zimenezi pophunzitsa mokhulupirika chiphunzitso cholondola cha m'Baibulo ku mpingo. Ndipo mungateteze nkhosa mwa kuvumbula ndi kutsutsa kupatuka kulikonse pachowonadi cha Mau a Mulungu.[6]

Mbusa wa Chipentekoste adziwike ngati mwamuna kapena mkazi wa Buku. Ayenera kukhulupirira kuti Baibulo linauziridwa ndi Mulungu. Chifukwa cha zimenezi, ayenera kuyamikira Baibulo ndi kulilemekeza kwambiri. Ayenera kudziwa Mau a Mulungu ndi kuphunzitsa mwakhama ndi kulalikira malangizo ake kwa anthu a Mulungu

[6] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kuteteza nkhosa, onani Mutu 27: "Kuteteza Nkhosa."

~ Mutu 10 ~

Amalimbikitsa Choonadi cha Chipentekoste

Mbusa wa Chipentekoste aliyense mu Afirika ayenera kulimbikitsa choonadi cha Chipentekoste mu mpingo umene iyeyo amatumikira. Kuti achite ichi, ayenera kumvetsetsa bwino ziphunzitso zoona za m'Baibulo zofotokozera za Chipentekoste monga bungwe la uzimu. Ndipo ayenera kumafotokoza bwino zoonadi zimenezi.

Nkhani yake ikuposa kungopambana pa mtsutsano wa za mau a Mulungu. Zikukhudzanso kukwaniritsa Lamulo Lalikulu la Utumwi mopambana. M'mene wina amaonera ntchito ya Mzimu Woyera m'miyoyo ya okhulupirira imakhudzanso mwapadera m'mene iyeyo angakhalire wofuna kukwaniritsa Lamulo la Khristu lokapanga ophunzira ku mafuko onse (Mateyu 28:18-20). Popanda kumvetsetsa bwino za ntchito yopereka mphamvu ya Mzimu Woyera kukwaniritsa Lamulo Lalikulu la Utumwi kudzakhala kosatheka.

Taganizani kukhala ndi sizasi imene ili ndi kampeni kamodzi kokha. Ngakhale itakhala yakuthwa bwanji, koma singagwire ntchito iliyonse. Koma mipeni iwiri ya sizasi itakumana, sizasi imakhala chida chodalirika. Momwemonso ndi chiphunzitso cha m'Baibulo pantchito ya Mzimu Woyera. Ngati wina angatsindike ntchito yopulumutsa ya Mzimu Woyera (monga zalembedwera mu makalata a Paulo), nkuchotsapo ntchito yake ya Mzimu Woyera

yopereka mphamvu (monga zalembadwera mu Machitidwe), machitachita a Mzimu Woyera m'miyoyo ya okhulupirira amachepetsedwa, komanso ntchito ya ufumu imakhala yopanda mphamvu. Koma pamene fundo zonse ziwiri zaikidwa pamodzi, kumvetsetsa kwabwino kwa ntchito ya Mzimu Woyera kumatumphuka. Zotsatira zake, anthu a Mulungu amakumana ndi Mzimu wa Mulungu monga Iyeyo adafunira. Ndipo amathandizidwa kuti apititse ufumu wa Mulungu patsogolo mdziko lapansi mopambana.

Mutu uwu ndi okhudza udindo wa mbusa wa Chipentekoste wolimbikitsa choonadi cha Chipentekoste mu mpingo. Ponena za choonadi cha Chipentekoste, tikutanthauza zoonadi zija za m'Baibulo ndi machitachita zimene akatswiri a sukulu a Chipentekoste amatsindikiza. Zoonadi zimenezi zikukhudza umunthu ndi ntchito ya Mzimu Woyera m'miyoyo ya okhulupirira.

Ngati gulu la Chipentekoste mu Afirika lingakhalebe ndi changu cha kulalikira komanso utumwi, abusa a Chipentekoste ayeneranso kulimbikitsa mokhulupirika chiphunzitso cha Chipentekoste ndi machitachita ake mu mpingo. Koma ngati angalephere mu ncthito imeneyi, bungwe la Chipentekoste lidzatsimphina ndi kucheperachepera, monganso adachitira magulu ena m'mbuyomu. Mipingo yawo ikhoza kukhalabe ndi mamvekedwe a Chipentekoste; koma mipingoyo idzataya mphamvu za uzimu komanso changu cha utumwi. Zikatero udzakhala mpingo wina wokhala ndi mbiri yakale koma wopanda mphamvu mu nthawi ino (2 Timoteo 3:5).

KUMVETSETSA MAZIKO

Akatswiri a Sukulu a Chipentekoste amayang'ana malemba onse monga maziko a ziphunzitso zawo. Komano, gwero lawo loyambirira pomvetsetsa ntchito yopereka mphamvu ya Mzimu Woyera ndi buku la Chipangano cha Tsopano la Machitidwe. M'buku limeneli amapezamo chilimbikitso, chizindikiritso cha m'mene Mzimu Woyera amadzadzira, kupereka mphamvu, ndi kugwiritsa ntchito anthu ku utumiki wa ufumu.

Maganizidwe a za mau a Mulungu a Chipentekoste amene amasiyanitsa a katswiri a sukulu a Chipentekoste, ndi iwo amene si a Chipentekoste, ndi m'mene ali yense wa iwowa amalifikira buku la Machitidwe. Amene si a Chipentekoste amawerenga buku la Machitidwe monga mbiri yopatulika. Kwa iwowo, bukulilimafotokoza nkhani ya uzimu youzilidwa ya m'mene mpingo wa ku Yerusalemu mu zaka zana zoyambirira unayambira ndi m'mene unafalikira mu

ufumu wa Chiroma. Munjira yina kwa amene si a Chipentekoste, buku la Machitidwe limaonedwa monga mbiri chabe, ndi kuwerenganso kwa nkhani zimene zinachitika nthawi imeneyo kumeneko mu zaka zana zoyambirira.

A Chipentekoste, mbali inayi, amaona Machitidwe mosiyana kwambiri. Amabvomerezana ndi ena a chi Evangeli kuti buku la Machitidwe limafotokoza molondola mbiri ya mpingo woyamba. Komano amaliona bukuli monga loposa mbiri yopatulika. Iwo a Chipentekoste amakhulupirira kuti Luka adalemba buku la Machitidwe kuti apereke ku mpingo chitsanzo cha m'mene mpingo uzichitira mpaka kubweranso kwa Khristu. Machitidwe motero amatipatsa ife chitsanzo chokhazikika cha m'mene a Khristuazikhalira moyo wawo ndi kutumikira kuno ndi panopa. Kuchokera mu Machitidwe timaphaunzira kuti Mpingo ulipo kuti unyamule umboni wa Khristu mopatsidwa mphamvu ndi Mzimu kumudzi ndi ku malekezero adziko lapansi (Machitidwe 1:8).

Buku la Machitidwe likupitilirabe kufotokozera za m'mene ophunzira oyamba a Khristu anabatizidwira mwa Mzimu Woyera, komanso m'mene ubatizowo unasinthira miyoyo yawo ndi utumiki modabwitsa. Likuonetsera mpingo ukukwaniritsa utumiki wake mu mphamvu ya Mzimu Woyera ndi zizindikiro zakutsatapo (5:12-16; 6:8; 15:12). Mu Machitidwe, Mzimu akuitana, kupereka mphamvu, ndi kutuma akapolo a Khristu kuti akalalikire uthenga wa chipulumutso molimbika mtima. Pamene iwo akumvera, Mzimu akuwatsogolera panjira yawo molunjika bwino. Nthito yawo ya utumwi ikuchitika motsagana ndi matsanulidwe a Mzimu Woyera (2:4; 4:31).

Ntchito ya utumwi ya Mzimu Woyera mu Machitidwe, imaonetsa mbusa wa Chipentekoste chithunzithunzi chabwino cha m'mene mpingo wa Chipentekoste uyenera kuonekera lero lino.

KUPITITSA PATSOGOLO "ZAPADERA" ZA CHIPENTEKOSTE

A Chipentekoste amatsimikizanso kuti buku la Machitidwe limapereka ku mpingo mlozo wa m'mene munthu angalandilire Mzimu Woyera. Ubatizo wa Mzimu umalandilidwa motsagana ndi kubadwanso mwatsopano. Malandilidwe ake amatsagana ndi chizindikilo cha utumwi cholankhula ndi malilime ena monga Mzimu alankhulitsa. Tiyeni mwachidule tiunike zikhalidwe za Chipentekoste zimenezi.

Chiphunzitso Cha Kutsatizana

Chiphunzitso cha kutsatizana chimati ubatizo wa Mzimu Woyera "ndi chinthu chapadera chosiyana ndi kubadwa mwatsopano.[1] Iwo amene si a Chipentekoste amaona kubadwa mwatsopano ndi ubatizo wa Mzimu monga magawo awiri a chipulumutso chomwecho. A Chipentekoste, mbali inayi amaona kuti ndi zinthu ziwiri zosiyana. Amene ndi a Chipentekoste amalozera za m'mene choonadi ichi chikuonetsedwa momveka bwino pamalo atatu mu buku la Machitidwe:

1. Kulandira Mzimu mu Samaryia (Machitidwe 8:4-17). Mu nkhaniyi, Filipo anatsikira ku Samariya ndipo analalikira Khristu kwai wo. Anthu anamvetsera mwachidwi ku zonena zake, nakhulupirira uthenga, anamasulidwa ku ukapolo wa ziwanda, nadzadzidwa ndi chimwemwe chachikulu, ndipo anabatizidwa m'madzi (vv.5-8, 12). Komabe, sipanapite masiku ambiri, pamene Petro ndi Yohane anafika ku Samariya, ndipo anasanjika manja awo pa iwo ndipo analandira Mzimu Woyera (vv.14-17).

2. Saulo (Paulo) alandira Mzimu (Mach. 9:1-19). Saulo anakumana ndi Yesu panjira ya ku Damasiko. Panthawi yomweyo iye anakhulupirira pa Yesu ndipo kawiri konse anamtchula Iye "Ambuye" (v.5; 22:8-10). Kenako iye anadzalemba, "Palibe munthu akhoza kunena, Yesu ali Ambuye, koma mwa Mzimu Woyera" (1 Akorinto 12:3). Saulo nthawi yomweyo anadzipereka yekha kwa Khristu namvera lamulo la Ambuye wake watsopano kuti alowe mu mzinda (Machitidwe 9: 6-9). Kumeneko anakumana ndi Ananiya, amene anamuitana iye, "mbale Saulo" (v.17; 22:13). Patapita masiku atatu, pamene Ananiya anaika manja ake pa iye, Saulo analandira Mzimu Woyera (vv.17-18).

3. Ophunzira khumi ndi awiri aku Efeso alandira Mzimu (Machitidwe 19:1-7). Amuna amenewa akuyenera kuti anali mamembala a mpingo umene umayamba kumene mu Efeso (18:27). Mau akuwatchula iwo "ophunzira" (v. 1). Anakhulupirira uthenga wa Yohane Mbatizi wokhudza kubwera kwa Ambuye Yesu, ndipo anali ataika chikhulupiriro chawo mwa Khristu ku chipulumutso. Choncho, Paulo, anawabatiza iwo m'madzi (v.5). Zinali zitatha izi zonse pamene

[1] Kuchokera mu Chiganizo cha Chikhulupiriro cha Chiyanjano cha Mpingo wa Assemblies of God pa dziko lonse, Nsanamira 9: "Ubatizo wa Mzimu Woyera" (onani Zowonjezera 2).

Paulo anaika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera anadza pa iwo, ndipo analankhula ndi malilime nanenera (v. 6).

Mu zitsanzo zonse zitatuzi, panali nthawi yomwe inapitapo pakati pa kupulumutsidwa kwa anthu ndi kubatizidwa kwawo mwa Mzimu Woyera. Kupitilira apo, cholinga cha ubatizo wa mphamvu ya Mzimu Woyera mkuganiza kwabwino, chiyenera kukhala chapadera chosiyana komano chotsagana ndi kubadwa mwatsopano (Machitidwe 1:8).

Chiphunzitso cha Malilime a Chitsimikizo

Iwo a Chipentekoste amaphunzitsanso kuti ubatizo wa Mzimu Woyera "umalandilidwa mwa chikhulupiriro, ndipo umatsagana ndi chizindikiro cholankhula ndi malilime ena monga Mzimuamalankhulitsa, monga chitsimikizo choyamba."[2] Monga mwa chiphunzitso chotsatizana, a Chipentekoste amatenga chiphunzitso chawo cha malilime achitsimikizo kuchokera mu kusanthula mau a m'buku la Machitidwe.

Kokwana kasanu bukuli likufotokoza za anthu akudzazidwa ndi, kapena kubatizidwa mwa Mzimu Woyera. Pa malo atatu a malo asanuwa, mau akuonetsa kuti iwo amene analandira Mzimu Woyera analankhula ndi malilime ena monga chotsatira cha kudzazidwa kwawo ndi Mzimu. Chitsanzo choyamba chinachitika pa Tsiku la Pentekosite pamene ophunzira okwana zana limodzi ndi makumi awiri anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo analankhula ndi malilime ena monga Mzimu anawalankhulitsa (Mach. 2:4). Chachiwiri chinachitika kunyumba ya Koneriyo mu mzinda wa m'mbali mwa nyanja ku Kayisaleya. Baibulo likuti iwo amene analipo "anadabwa powona kuti mphatso ya Mzimu Woyerainatsanulidwa ngakhale pa Amitundu. Pakuti anawamva akulankhula m'malilime nalemekeza Mulungu" (10: 45-46). Chitsanzo chachitatu chinachitika mu mzinda wa Efeso, kumene Paulo anakumana ndi ophunzira khumi ndi awiri. Baibulo likuti "Pamene Paulo anaika manja ake pa iwo, Mzimu Woyera anadza pa iwo, ndipo analankhula ndi malilime nanenera" (19:6).

Mu zitsanzo ziwiri zomalizirazi za anthu akudzazidwa ndi Mzimu Woyera mu Machitidwe, lemba likusonyeza mwamphamvu kuti iwo amene analandira

[2] Kuchokera mu Chiganizo cha Chikhulupiriro cha Chiyanjano cha Mpingo wa Assemblies of God pa dziko lonse, Nsanamira 9: "Ubatizo wa Mzimu Woyera" (onani Zowonjezera 2).

mphatsoyo analankhula ndi malilime. Mu chitsanzo choyamba, okhulupirira atsopano mu Samaria analandira Mzimu pamene atumwi, Petro ndi Yohane anaika manja awo pa iwo (Machitidwe 8:17). Ngakhale kuti Luka sakunena monenetsa kuti analankhula ndi malilime, lembali likuonetsa kuti chinachake chodabwitsa ndi chotsimikizika chidachitika. Simoni wanyanga anali ndi chidwi kwambiri kotero kuti anapempha kuti agule mphatsoyo. Akatswiri a Sukulu ya Baibulo amavomerezana kuti chizindikiro chomwe Simoni anachiona chinali choti okhulupirira atsopanowa analankhula m'malilime, poti chimenechi ndi chizindikiro chokhacho cholandirira Mzimu chomwe chikutchulidwanso madera ena mu Machitidwe.

Chitsanzo chomaliza cha munthu kudzazidwa ndi Mzimu mu Machitidwe chinali pamene wophunzira wotchedwa Ananiya anaika manja ake pa Saulo wa ku Tariso ndipo anapemphera ndi iye kuti adzazidwe ndi Mzimu (Machitidwe 9:17-18). Pamene lemba silikunena kuti Saulo analankhula m'malilime pa nthawi imeneyi, Paulo anachita umboni pa nthawi ina yake kuti iye amapemphera m'malilime kawirikawiri (1 Akorinto 14:18). Ndi zosakaikitsa kuti kulankhula m'malilime anayamba pa nthawi yomwe iye anapempherered wa.

Pachifukwa ichi ndi zina, Akatswiri a Sukulu ya Baibulo a Chipentekoste amanenetsa kuti ali yense wofunafuna Mzimu Woyera wopereka mphamvu, ayeneranso kuyembekeza kulankhula ndi malilime akangodzazidwa.

KULALIKIRA "UTHENGA ONSE"

Njira imodzi imene mbusa wa Chipentekoste angapititsire patsogolo choonadi cha Chipentekoste mu mpingo wake, ndi potsindika kawirikawiri "Uthenga Onse" mu chiphunzitso ndi ulaliki wake. Mau oti "Uthengu Onse" amakamba zachiganizo cha mau a Mulungu chimene anachigwira a Chipentekoste oyamba. Chiganizo chimenechi chimatchulidwanso kuti "Magawo Anayi a Uthenga Wabwino", kapenanso, kuti "Ngodya Zinayi za Uthenga Wabwino". Atsogoleri oyamba a Chipentekoste anachitambasula chiganizochi kuti atsindike chomwe iwo amakhulupirira kuti ndipo pamtima pa Uthenga wa Mpingo.

Nsanamira zinayi za Uthenga Onse zimaikidwa mu mau anayi motere: Yesu amapulumutsa; Yesu amachiritsa; Yesu amabatiza mwa Mzimu Woyera; Yesu akubweranso. Iwo a Chipentekoste oyambirira anamva mkati mwawo kuti ziphunzitso zofunikira zinayi izi zimalekererredwa ndi mpingo, ndipo kuti zinasoweka kuti zizitsindikizidwa. Mphamvu yaikulu ya chitsanzo ichi, ndi

chakuti chimamuika Yesu pakatimpakati pa ulaliki wathu ndi chiphunzitso chathu. Mu nthawi ino pamene mipingo yambiri ya Chipentekoste kuzungulira Afirika yataya njira yawo, kukhoza kukhala kwabwino kwa a Chipentekoste kubwereranso ku zotsindika zinayizi:

Yesu Amapulumutsa

Nsanamira yoyamba ya Uthenga Wabwino Wamphumphu ndi choonadi chakuti Yesu amapulumutsa. Iye yekha ndi Mwana wa Mulungu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi (Yohane 20:31; 1 Yohane 4:14). A Chipentekoste chotero amakhulupirira kuti chiyembekezo chokhacho cha chipulumutso cha munthu, ndi mwazi wokhetsedwa wa Yesu pa mtanda (Machitidwe 4:12; Akolose 1:20). Mbusa wa Chipentekoste aliyense woona adzalalikira kawirikawiri za mtanda wa Khristu, kuwamema anthu kuti "alape ndikukhulupirira uthenga wabwino" (Marko 1:15).

Yesu Amachiritsa

Nsanamira ya chiwiri ya Uthenga Onse ndi choonadi choti Yesu amachilitsa. A Chipentekoste amakhulupirira kuti lonjezo la machilitso auzimu lakhazikika pa mtima pa uthenga wabwino. Amakhulupiriranso kuti chipulumutso ku tchimo komanso mamasulidwe ku nthenda zaperekedwa pamodzi mu chiombolo. Machilitso otero ndi ufulu wa okhulupirira onse (Yes. 53:4-5; Mat. 8:16-17). Chifukwa cha ichi, iwo amalalikira molimbika mtima, "Yesu Khristu, ali yemweyo, dzulo ndi lero, ndi kunthawi zonse" (Ahebri 13:8). Monga Iye anapulumutsa ndi kuchilitsa anthum'Baibulo, amapulumutsa ndi kuchilitsa anthu lero.

Yesu Amabatiza mwa Mzimu Woyera

Nsanamira yachitatu ya Uthenga Onse ndi choonadi chakuti Yesu amabatiza okhulupirira mwa Mzimu Woyera, kuwapatsa mphamvu monga mboni zake kwa otaika (Machitidwe 1:8). Iwo a Chipentekoste amalalikira molimba mtima kuti okhulupirira onse ali ndi ufulu komanso ayenera kufunafuna mwa changu kubatizidwa mwa Mzimu Woyera molingana ndi Lamulo la Khristu (vv.4-5; fanizilani Luka 24:49).

Monga zakambidwa pamwambapo, chochitika ichi nchosiyana ndi kubadwanso mwatsopano, ndipo chimatsimikizidwa ndichizindikiro choyambirira

chooneka ndi maso cholankhula ndi malilime ena monga Mzimu wa Mulungu amalankhulitsa (Machitidwe 2:4). Mbusa ali yense wa Chipentekoste ayenerakumalalikira pafupipafupi za ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipoazipemphera ndi anthu ake kuti adzazidwe.[3]

Yesu Akubweranso

Nsanamira ya chinayi ya Uthenga Onse ndi choonadi choti Yesu akubweranso. Yesu analonjeza kuti adzabweranso kuchokera kumwamba kudzatenga anthu ake kuti akakhale ndi Iye (Yohane 14:3). Pobwera Iye, onse akufa mwa Khristu adzaukitsidwa iwowo. Kenako, onse omwe adzakhale adakali moyo pa nthawiyo adzakwatulidwa pamodzi kukakumana ndi Ambuye (1 Ate. 4:16-17; 1 Ako. 15:51-52). Ichi ndi chiyembekezo chodala cha Mpingo (Tito 2:13).

Iwo amene amamdziwa Khristu monga Mpulumutsi wawo, ndipo akukhala moyo wokhulupirika omvera, amalandira uthenga wa kubweranso kwa Khristu ndi chimwemwe. Koma iwo amene amakana Khristu, amaulandira uthengawo ndi mantha. Mbusa wa Chipentekoste ayenera kulalikira molimba mtima uthenga wakubweranso kwa Khristu kwa anthu onse, kuwaitanila iwo kuti alape machimo onse ndi zadziko zonse, ndikuyenda moyo wachiyero. Chidziwitso choti Khristu akubwera posachedwa chimatakasa a Khristu a Chipentekoste kugwira ntchito ndi cholinga choti aoneanthu otaika akubwera kwa Khristu.

UTUMIKI WA CHIPENTEKOSTE

Mbusa wanzeru wa Chipentekoste amamvetsetsa kuti moyo wa Chipentekoste ndi utumiki zimakula mosavutikira kudzera mu kumvera choonadi cha Chipentekoste. Iyeyo amamvetsetsa kuti "Chikhulupiriro cha anthu sichiyenera kutsamira pa nzeru ya munthu, koma pa mphamvu ya Mulungu" (1 Ako. 2:4-5). Chikhulupiriro cholondola chimatsogolera ku zochita zoyenera, ndipo chikhulupiriro cholondola ndi ntchito zizitsogolera ku makhalidwe olondolanso. Tiyeni tione zitsanzo zisanu za moyo wa Chipentekoste ndi utumiki zimene zimachokera kukumvera choonadi cha Chipentekoste:

[3] Zambiri zokhudza kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera onani mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu Woyera."

Moyo Wodzazidwa ndi Mzimu

Moyo wodzazidwa ndi Mzimu ndi chotsatira cha chidziwikire cha moyo wotsamira pa choonadi cha Chipentekoste. Pamenemukulalikira ndi kupemphera ndi anthu kuti adzazidwe ndi Mzimu, Mzimu wa Mulungu adzayamba kugwira ntchito m'miyoyo yawo. Iye adzayamba kuwaumba iwo kuti akhale antchito a Khristu opambana. Mukuyenera kugwiritsa ntchito mwayi umenewu powatsogolera anthu kuti ayende m'moyo wodzazidwa ndi Mzimu.[4]

Pemphero Lotsogodzedwa ndi Mzimu

Kulalikira ndi kuphunzitsa choonadi cha Chipentekoste pa guwa chidzatsogolera ku pemphero lotsogozedwa ndi Mzimu mu mpingo. Pamene mukutsogolera mamembala ku moyo wodzazidwa ndi Mzimu, ndikuwaphunzitsa kupemphera mwa Mzimu, khalidwe lawo la pemphero lidzasinthika. Adzayamba kumapemphera mwamphamvu, mapemphero otsogodzedwa ndi Mzimu. Paulo analankhula za pemphero la mtundu umenewo mu Aroma 8:26-27 (fanizilani 1 Akorinto 14:14-15; Aefeso 6:18).[5]

Kuchitira Umboni mwa Mphamvu

Yesu adalonjeza, "Komatu mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga" (Mach. 1:8). Pamene anthu adzazidwa ndi Mzimu ndipo atsogoleredwa kukholola, adzayamba kuchitira umboni ndi changu chachikulu komanso mwamphamvu kuposa kale. Komanso mpofunika kugwiritsa ntchito mwayi umenewu powatsogolera anthu mu kuchitira umboni, kudzala mpingo, ndi machitachita ena ofalitsa uthenga wabwino.

Mphatso za Uzimu

Kuphunzitsa mokhulupirika choonadi cha Chipentekoste mu mpingo chidzalimbikitsanso chionetsero cha mphatso za uzimu. Monga mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kulimbikitsa chizolowezi chotere mu mpingo pophunzitsa pa mutu umenewu.[6] Kuonjezera apo mukuyenera kumapereka nthawi

[4] Bulu lotchedwa, *Kuyenda Naye Mzimu,* likupezeka mwaulere kuchokera pa tsamba la www.decadeofpentecost.org.

[5] Pa zambiri zakuphunzitsa mamembala ampingo pemphero, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

[6] Onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akoronto 12:8-10."

ya chionetsero cha mphatso za uzimu m'misonkhano ya mpingo. Mukhonzanso kupita patsogolo polimbikitsa machitachita a mphatso za uzimu pokola Mzimu kugwira ntchito mwa inu ndi kupyolera mwa inu. Machitachita a mphatso za uzimu mu mpingo adzapangitsa kuti anthu ochuluka apulumutsidwe, achilitsidwe, ndikudzazidwa ndi Mzimu.

Masomphenya a Utumwi

Pomaliza, pamene mukuphunzitsa mokhulupirika choonadi cha Chipentekoste kwa anthu, masomphenya a utumwi adzalengeka mu mpingo. Pamene mamembala akudzazidwa ndi Mzimu naphunzitsidwa udindo wawo wokapanga ophunzira a mitundu yonse, mitima yawo idzayatsidwa ndi chifundo cha chipulumutso cha anthu kuli konse. Muyenera kulimbikitsa masomphenya amenewa pokhazikitsa ndondomeko ya utumwi mu mpingo.[7]

Mpingo wa Chipentekoste lero umayang'ana ku mpingo wa m'buku la Machitidwe monga chitsanzo cha utumwi wodzozedwa ndi Mzimu ndi machitachita ake. Umatakasika ndi changu chachikulu cha utumwi cha Mpingo woyamba ndipo umapezako njira ya mphamvu yofikira otaika ndi uthenga wabwino. M'masiku ano otsiriza Yesu asanabwerenso, abusa a Chipentekoste ayenera kukhaladi a Chipentekoste mu chikhulupiriro, chikhalidwe, ndi mu ntchito. Ndipo ayenera kuphunzitsa anthu awo kukhala monganso iwo.

[7] Zambiri zokhudzana ndi phunziroli, onani Mutu 40: "Kukhazikitsa Dongosolo la Utumwi la Mpingo Wapamalo."

~ Mutu 11 ~

Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekoste

Mbusa wa nzeru wa Chipentekoste adati, “Ndi chinthu chinakukhala wa Chipentekoste wolalika, komanso ndi chinthu china kukhala mlaliki wa Chipentekosite.” Fundo imene mbusayu amafuna kunena ndi yakuti, mlaliki akhoza kukhala wa Chipentekoste mwa dzina chabe osakhala wa Chipentekoste mu ntchito. Mbusa akhoza kukhala gawo la mpingo wa Chipentekoste ndithu koma asakulabadira moyo wa Chipentekoste ndi ntchito zake. Koma mbusa weniweni wa Chipentekoste adzalimbikitsa mokhulupirika moyo wa Chipentekoste ndi ntchito zake mu mpingo womwe iye amautsogolera.

Mu mutu wapitawo, tinaona udindo wa mbusa wa Chipentekoste wolimbikitsa choonadi cha Chipentekoste. Mu mutu uno, tikambilana za udindo wake wolimbikitsa moyo wa Chipentekoste ndi ntchito zake.

AMALIMBIKITSA MOYO WA CHIPENTEKOSTE

Anthu a Chipentekoste amakakamira kuti, pamene kukhulupirira Mulungu kuli kofunika, pakokha sikokwanira. Kawirikawiri amaloza ku mau a Yakobo: “Ukhulupirira iwe kuti Mulungu ali m’modzi; uchita bwino; ziwanda zimakhulupiriranso, ndipo zinthunthumira” (Yakobo 2:19).

Iwo a Chipentekoste amaphunzitsa kuti, kuposera pokhulupirira chabe Mulungu, munthu ayenera kukhala ndi ubale wapadera ndi Mulungu. Ubale umenewo umakhazikika ndi kulimbikitsidwa kudzera mukukumana ndi Mulungu kwa munthu payekha. Katatu ka kukumana ndi Mulungu kameneka ndiko, kubadwa mwatsopano, ubatizo wa Mzimu, ndi chiyanjano cha tsiku lililonse ndi Khristu. Tiyeni tiwone mwatsatanetsatane za zinthu zitatuzi ndi m'mene inuyo, monga mbusa wa Chipentekoste, mungapititsire patsogolo okumana ndi Mulungu amenewa mu mpingo umene Khristu anakusankhirani kuti muutsogolere:

Kubadwa Mwatsopano

Choyambirira, muyenera kutsindika za kufunika kobadwa mwatsopano mu ulaliki ndi chiphunzitso chanu. Muyenera kuonetsetsa kuti membala aliyense wa mpingo wabadwa kuchokera kumwamba. Komanso muzionetsetsa kuti aliyense wobwera ku mpingo wanu wauzidwa zolandira Khristu monga Mpulumutsi. Ichi ndi chimene Yesu adachita ndi Nikodimo. Adamutsimikizira mtsogoleri wa chipembedzoyu, "Uyenera kubadwa mwatsopano" (Yohane 3:7). Mau awa a Yesu azikhala kawirikawiri pa milomo yanu pamene muphunzitsa ndi kulalikira.

Kubadwa mwatsopano ndiko "kubadwa mwa Mulungu" (Yohane 1:13; fanizilani 3:5,8). Munthu amabadwa mwa Mulungu pamene abwera kwa Khristu modzichepetsa, navomereza Iye monga Mbuye ndi Mpulumutsi, kulapa machimo ake onse, naika chikhulupiriro chake chonse mwa Iye ku kukhululukidwa ndi chiyeretso. Panthawi imeneyi, kusandulika kosintha moyo kumachitika. Khristu amalowa mu moyo wake ndipo Mzimu Woyera amamusintha munthuyo kuchokera mkati. Paulo adalemba, "Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano" (2 Akorinto 5:17).

Ubatizo wa Mzimu

Kuonjezera zotsogolera anthu ku kubadwanso mwatsopano, monga mbusa wa Chipentekoste wokhulupirika, muyenera kuwalimbikitsa anthu amene alandira Yesu monga Mpulumutsi, kuti mwachangu abatizidwe mwa Mzimu Woyera. Ichi ndiye chinali chizolowezi cha Mpingo woyamba. Pamene atumwi ku Yerusalemu anamva kuti anthu anapulumutsidwa mu Samaria, nthawi yomweyo anatuma Petro ndi Yohane kuti akawapempherere kuti alandire Mzimu Woyera (Machitidwe 8:14-17). Patapita zaka, pamene Paulo anafika ku Efeso, funso loyamba limene anafunsa ophunzirakumeneko linali loti, "Kodi munalandira

Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?" (19:2). Pamene mtumwi anazindikira kuti sanalandire Mzimu, nthawi yomweyo anaika manja ake pa iwo, ndipo "Mzimu Woyera anadza pa iwo, ndipo analankhula ndi malilime ena, nanenera" (v. 6).

Monga mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutsatira chitsanzo cha atumwi ndi kulimbikira kuonetsetsa kuti Mkhristu ali yense watsopano mwachangu wabatizidwa mwa Mzimu Woyera. Muyeneranso kuonetsetsa kuti ali yense amene walandira Mzimu, alinso ndi kumvetsetsa kwabwino kwa chifukwa chimene Mulungu amabatizira okhulupirira mwa Mzimu Woyera. Amawapatsa iwo Mzimu wake kuti awapatse mphamvu zokhala mboni zake za Khristu (Machitidwe 1:8). Choncho mudzayeneranso kuwalimbikitsa okhulupirira amene angodzazidwa kumene ndi Mzimu kuti azigawa Khristu molimba mtima ku mabanja awo ndi kwa azinzawo.

Kuti mukhazikitse mpingo weniweni wodzazidwa ndi Mzimu wautumwi, mudzasowekera kumalalikira ndi kuphunzitsa kawirikawiri za kufunikira kwa kuti wokhulupirira ali yense abatizidwe mwa Mzimu Woyera. Chiphunzitso chanu pa ubatizo wa Mzimu chiyenera kuyankha momveka bwino mafunso atatu: 1) Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi chiyani? 2) Nchifukwa chiyani wokhulupirira aliyense ayenera kubatizidwa mwa Mzimu Woyera? Komanso 3) Munthu angalandire bwanji Mzimu Woyera?[1]

Kupitirira apo, muyenera kupereka kwa iwo obwera ku mpingo mwayi wa pafupipafupi woti akhoza kudzazidwa kapena kudzazidwanso ndi Mzimu Woyera. Izi zikutanthauza kuti mudzayenera kupanga danga mu m'mapemphero a mu mpingo kuti okhulupirira afunefune Mulungu ndi kupempha Mzimu Woyera kwa Mulunguyo (Luka 11:3). Kuonjezera apo, muyenera kupanga zinthu zokonzekeretsa anthu mu mpingo kuti akhoza kulandira Mzimu mosavuta. Chikonzero chimenecho chidzaphatikizapo kupezeka koonekera kwa Mulungu

[1] Kuti mupeze ndondomeko ya ulaliki pa mutu umenewu, onani buku lotchedwa, *Kulalikira Chipentekoste: Ndondomeko zama Ulaliki 100 a Mphamvu ya Mzimu Woyera,* Ulaliki 2: "Ubatizo wa Mzimu Woyera." Bukuli litha kupezeka mwaulere kuchokera pa webusaiti ya www.DecadeofPentecost.org.

ndi kumvetsera kwa chiyembekezo kwa chikhulupiriro m'mitima ya anthu a Mulungu.[2]

Chiyanjano cha Tsiku ndi Tsiku

Pomaliza, muyenera kuonetsetsa kuti mamembala a m'mpingo mwanu akukhala moyo wawo muchiyanjano ndi Khristu tsiku lililonse. Yesu adatchula chizolowezi chimenechi monga, kukhala, kapena kukhalabe mwa Khristu (Yohane 15:4-7). Paulo adachitchula kuti kuyenda "limodzi ndi Mzimu" (Agalatiya 5:25). Choncho mukuyenera kuphunzitsa anthu kuti sizokwanira kungobadwa mwatsapano, kapenanso kubatizidwa ndi Mzimu. Akhristu akuyenera kudzipereka okha kukukhala m'moyo wachiyanjano chosaphwanyika ndi Khristu kupyolera mwa Mzimu Woyera (fanizilani Yohane 14:16-18, 23; 1 Yohane 1:3).

- Kudzera mu mau ndi chitsanzo, muyenera kuphunzitsa anthu a Mulungu m'mene angachitire zinthu izi:
- Kuyenda "limodzi ndi Mzimu" (Agalatiya 5:25).
- Kukhala monga mwa Mzimu" pokhazika "maganizo awo pa zimene Mzimu amazifuna" (Aroma 8:5-6).
- Kumulandira Mzimu wa Mulungu kuti aziyenda nawo monga Wowayankhulira, Mthandizi, komanso Nkhoswe yawo (Yohane 14:16).
- "Kupemphera mwa Mzimu nthawi zonse ndi mapemphero a mitundu yonse ndi zopembedzera" (Aefeso 6:18; fanizilani Aroma 8:26; Yuda 20).
- Kudalira pa Mzimu Woyera kuti awalitse maganizo awo ndi kutakasa mitima yawo pamene akulingalira pa Malemba (Yohane 16:13).
- Kukulitsa chipatso cha Mzimu m'miyoyo yawo (Agalatiya 5:22-23).

Kuti zolinga izi zikwanilitsidwe, mukuyenera kuphunzitsa mwachangu anthu a Mulungu zimene Malemba amanena za moyo wodzazidwa ndi Mzimu. Mudzayeneranso kukhala chitsanzo cha zimenezi m'moyo wanu ndi utumiki wanu.

[2] Pa zambiri zakukonzekeretsa okhulupirira kulandira Mzimu Woyera, onani buku, *Kusonkhanitsa ku Utumwi, Mutu* 7: "Kodi tingalalikire bwanji za Ubatizo wa Mzimu Woyera." Likupezeka mwaulere kuchokera pa webusaiti ya www.DecadeofPentecost.org.

AMALIMBIKITSA NTCHITO ZA CHIPENTEKOSTE

Pamodzi ndi kutsogolera anthu a Mulungu ku moyo wa Chipentekoste, inuyo, monga mbusa wa Chipentekoste, muyeneranso kuwatsogolera mu ntchito kapena zizolowezi zotsimikizika za Chipentekoste. Kuti muchite izi, muyenera kudzipereka nokha kukulimbikitsa ntchito khumi zomwe zili pa mtima pa Chipentekoste mu mpingo mwanu:

Kukalikira Kodzozedwa

Choyamba, monga mbusa wa Chipentekoste, muyenera kudzipereka nokha kukulalikira kodzozedwa kwa mau a Mulungu. Kudzoza ndi kupezeka kwa Mulungu koonekera kumene kumadza pa wophunzira wodzazidwa ndi Mzimu, kumuthandiza iyeyo kutumikira ndi mphamvu yaikulu komanso mopambana. Pofunafuna kudzoza, mudzakhala mukutsatira chitsanzo cha Yesu ndi atumwi. Yesu adati zaulaliki wa Iye yekha, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa Iye wandidzoza kulalikira uthenga wabwino" (Luka 4:18). Atumwi nawonso analalikira pansi pakudzoza kwa Mzimu Woyera (Machitidwe 2:14-18; 4:8; 13:8-12).

Mukhoza kutsimikiza za kudzoza kwa Mzimu pomuitana Iye kuti abwere pa inu pamene mukutumikira Mau a Mulungu. Ndipo pamene Wabwera, mudzayenera kuyankha mwa chikhulupiriro polalikira molimba mtima Mau a Mulungu (Machitidwe 4:31). Yesu adalonjeza kutsimikiza Mau olalikidwa mwa kudzoza ndi zizindikiro zozizwa (Marko 16:15-18).

Pemphero la Odwala

Chachiwiri, monga mbusa wa Chipentekoste weniweni, muyenera kudzipereka ku kupempherera odwala ndi osautsidwa pokhulupirira Mulungu za machilitso auzimu. Yesu adatuma ophunzira ake khumi ndi awiri ndi lamulo: "Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, tulutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere" (Mateyu 10:8). Yakobo analangiza atsogoleri a mpingo, "Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akulu a Mpingo apemphere pa iye, atamdzoza ndi mafuta m'dzina la Ambuye. Ndipo pemphero la

chikhulupiriro lidzapulumutsa [lidzachiritsa] wodwalayo, ndipo Ambuye adzamuukitsa" (Yakobo 5:14-15).[3]

Kutenga nawo Mbali pa Utumwi

Chachitatu, monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuonetsetsa kuti kutenga nawo mbali pa utumwi chikhale cholinga cha pamwamba cha mpingo wanu. Kutenga nawo mbali pa utumwi modzipereka chili pa phata pa chimene chimatanthauza kukhala wa Chipentekoste. Yesu adalumikiza Pentekoste ndi utumwi pamene Iye adauza ophunzira ake, "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko" (Machitidwe1:8). Mpingo sungadzitchule wokha motsimikiza kuti ndi wa Chipentekoste pamene nthawi yomweyo ukupewakuchita utumwi. Monga mbusa wa Chipentekoste, muli ndi udindo wokhazikitsa dongosolo la utumwi lochitachita mu mpingo.

Kuti muchite ichi, muyenera ku malalikira ndikuphunzitsa kawirikawiri pa utumwi wa Mulungu. Utumwi wa Mulungu ndi dongosolo lake lopulumutsa ndi kuitana anthu kwa Iye yekha kuchokera ku malilime onse, mtundu, ndi fuko pa dziko lapansi Yesu asanabwerenso (fanizilani Mateyu 24:14; Chivumbulutso 5:9). Muyenera kuonetsetsa kuti membala ali yense akumvetsetsa udindo wake wotenga nawo mbali mukukwaniritsa utumwi wa Mulungu.

Mudzayenera kupanga madanga oti mamembala a mpingo achite nawo utumwi aliyense payekha payekha. Mukhoza kuchita izi potsogolera anthu ku maulendo a utumwi afupiafupi, ku misonkhano ya pa mtetete, ulaliki wa m'miseu, ndi maulendo ena otere. Kuonjezera apo, mudzayenera kupanga dongosolo lapafupipafupi lodziwitsa mamembala za utumwi kumene iwo atha kubetcheledwa kuti apereke chuma chawo kuchikhazikitso cha utumwi cha mpingo. Mpingo uliwonse wa Chipentekoste uyenera kutengako atumwi kuti aziwathandiza ndi chuma chawo ndi mapemphero.[4]

---

[3] Pa zambiri zokhudzana ndi mutu umenewu, onani buku la Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Utumiki Wamphamvu: Mmene Tingatumikire mu Mphamvu ya Mzimu,* Mutu 11: "Tingachiritse Bwanji Odwala."

[4] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kulimbikitsa mpingo wanu ku utumwi, onani Mutu 40: "Kukhazikitsa Dongosolo la Utumwi la Mpingo Wapamalo."

Maitanidwe a Mulungu

Chachinayi, monga mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutsindika za maitanidwe a Mulungu ku utumiki. Maitanidwe a Mulungu ndi kusankha Kwake ndi kuitana anthu kwa Iye yekhakomanso ku zolinga Zake. Yesu, amene Iye yekha adatumidwa ndi Mulungu, panopa amaitana ndi kutuma ena ku kholola (Mateyu 4:19; Yohane 20:21). Adawauza ophunzira ake, "Inu simundisankhe, koma Ine ndinakusankhani inu kuti mupite ndi kubala chipatso" (Yohane 15:16).

Ngati mpingo wa Chipentekoste ungakule mopitilirabe (monga Mulungu adafunira), ukuyenera kukhala ndi polandirira odzala mipingo atsopano, abusa, atumwi, alaliki, ndi ena atumiki a uthenga wabwino otumikira moyo wawo wonse. Anthu amenewa akuyenera kukhala ochokera mu mipingo yathu ya Chipentekoste. Choncho muyenera kulimbikitsa anthu kumamvetsera ku maitanidwe a Mulungu. Ndipo pamene Iye alankhula, monga mneneri wakale adachitira, ayenera kuyankha, "Ndine pano, tumani ine!" (Yesaya 6:8).[5]

Nkhondo ya Uzimu

Chachisanu, monga mbusa wa Chipentekoste Mu Afirika, muyenera kukhala wokonzeka kuchita nkhondo ya uzimu. Nthawi zonse mukuyenera kukhala wokonzeka kulimbana ndi kugonjetsa mphamvu za ziwanda pamene zikudzionetsera. Izi ndi zimene Yesu ndi ophunzira ake adachita (Marko 16:16-18). Muyenera kukonzekeretsa mamembala anu kuchita chimodzimodzi.[6]

Kulambira Kwamphamvu

Chachisanu ndi chimodzi, muyenera kuonetsetsa kuti mpingo wanu ukupanga malambiro a mphamvu odzozedwa ndi Mzimu.Kulambira kotero ndiko kumazindikiritsa uzimu wa Chipentekoste. Iwo a Chipentekoste amadziwika ndi kulambira momasuka komanso moonetsera. Misonkhano yawo imakhala ndi

[5] Pa zambiri za maitanidwe aumulungu ku utumiki, onani mutu 1: "Munthu Okumana Ndizochitika." Ndondomeko ya maulaliki khumi ndi awiri pa maitanidwe a Mulungu akupezeka mu buku, *Kulalikira Khristu ku Maiko: Ndondomeko zama Ulaliki 100 pa Utumwi Opatsidwa Mphamvu,* Gawo 5: "Maitanidwe a Mulungu." Ma ulaliki amenewa akupezeka pa tsamba la www.DecadeofPentecost.org.

[6] Titha kupeza zambiri za izi pa mutu 22: "Kumenya Nkhondo za Uzimu." Onaninso buku la Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Utumiki Wamphamvu: Mmene Tingatumikire Mwamphamvu ya Mzimu, Mutu* 12: "Kutulutsa Ziwanda."

mayimbidwe odzipereka, kuomba m'manja, kuvina, ndi kukweza manja m'mwamba. Koma sizokwanira kuti mpingo wanu ukhale ndi kulambira kodzipereka; kuyenera kukhala kulambira kodzozedwa, ndipo kuzikhala kwenikweni. Yesu adalangiza ophunzira ake, "Mulungu ndi Mzimu, ndipo omulambira Iye ayenera kumulambira mu Mzimu ndi mchoonadi" (Yohane 4:24). Paulo adaonjezapo, "Pamene pali Mzimu wa Ambuye, pamakhala ufulu" (2 Akorinto 3:17).

Mu nthawi za kulambira, muyenera kulimbikitsa wolambira aliyense kuti azilunjika pa Mulungu ndi ukulu Wake. Ndiponso muyenera kulangiza anthu a Mulungu kuti atsegule mitima yawo kukuyenda kwa Mzimu wa Mulungu.[7]

Umboni wa Munthu Payekha

Chachisanu ndi chiwiri, muyenera kulimbikitsa mamembala a mpingo wanu kumaperekera umboni wawo kwa anzawo. Anthu a Mulungu nthawi zonse azikhala okonzeka kugawana ndi ena nkhani za zimene Mulungu wachita (1 Petro 3:15). Baibulo likulimbikitsa, owomboledwa a Ambuye anene nkhani yawo (Masalimo 107:2).

Umboni uli pa mtima pa chimene chimatanthauza kukhala mboni yake ya Khristu. Ndi njira yophweka koma yamphamvu kwambiri yomwe okhulupirira angagawire uthenga wabwino kwa otaika. Choncho muyenera kulimbikitsa chizolowezi ichi pakati pamamembala a mpingo. Ndipo muyenera kupanga danga mu m'mapemphero a mpingo kuti anthu a Mulungu azipereka umboni wa m'mene Mzimu akugwirira ntchito m'miyoyo yawo.

Mphatso za Uzimu

Chachisanu ndi chitatu, monga mbusa wa Chipentekoste,muyenera kulimbikitsa kuyenda kwa Mzimu mu mapemphero a mpingo kumene kumabweretsa maonetseredwe a mphatso za uzimu. Ichi chinali chizolowezi cha Mpingo woyamba, (mwachitsanzo, Machitidwe 11:28-30; 13:1-2; 21:10-14). Mu 1 Akorinto 12:8-10, Paulo akulankhula za mphatso zisanu ndi zinai za uzimu:

> "Kwa wina kwapatsidwa mwa Mzimu mau a nzeru, kwa wina mau a chidziwitso, monga mwa Mzimu yemweyo, kwa wina chikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo, kwa wina mphatso za machiritso mwa Mzimu mmodziyo;

[7] Pa zambiri zokhudza zimenezi, onani Mutu 18: "Kutsogolera Mpingo M'kulambira."

> kwa wina machitidwe a mphamvu; ndi kwa wina uneneri; kwa wina chizindikiritso cha mizimu, kwa wina malilime a mitundumitundu, kwa wina mamasulidwe a malilime. Izi zonse ndi ntchito ya Iye, ndi Mzimu mmodzi yemweyo, nagawira izo kwa yense monga Iyeyo afunira."[8]

Pamene muphunzitsa anthu kutumikira mu mphatso izi, mpingo udzamangilirika, Mulungu adzalemekezedwa, ndipo ufumu Wake udzapita patsogolo.

Mukuyenera kudziwa kuti makamaka, chionetsero cha mphatso za uzimu sizichitika mwa pompopompo. Mphatso zimachita kufunidwa, ndipo ziyenera kulimbikitsidwa (1 Akorinto 12:31;14:1). Choncho muyenera kulakalaka maonetsedwe a mphatso za uzimu m'moyo wanu womwe, ndiponso muzitakasa maonetsedwe a mphatsozi m'miyoyo ya ena. Mutha kuchita ichi pophunzitsa ndi kulalikira pamutu umenewu. Mukhozanso kulimbikitsa maonetsedwe a mphatso za uzimu popanga danga la mphatsozo mu mikumano ya mpingo (14:26) komanso pokhala tcheru kuti zisagwiritsidwe ntchito molakwika (14:39-40).[9]

Pemphero Lopembedzera

Chachisanu ndi chinayi, muyenera kutsogolera mpingo wanu mu pemphero lodzipereka lopembedzera. Monga mpingo wa m'buku la Machitidwe, mpingo wa Chipentekoste mu Afirika lero uyenera kukhala odzipereka ku pemphero (Machitidwe 1:14; 4:23-32;12:5;13:2). Monga Yesu anaphuzitsa ophunzira ake kupemphera, inunso muphunzitse anthu anu chimodzimodzi (Luka 11:1-13).Mutha kuchita ichi polalikira ndi kuphunzitsa kawirikawiri za pemphero, komanso pokhala wa pemphero pamanso pa mpingo. Anthu akamaona mbusa wawo akupemphera, iwonso adzalimbikitsidwa kupemphera (Luka 11:1; Eksdo 33:10).[10]

Moyo wa Chiyero

Chomaliza, monga mbusa wokhulipirika wa Chipentekoste, muyenera kulimbikitsa mamembala a mpingo wanu kuti azikhala moyo wachiyero, miyoyo yolemekeza Mulungu(1 Yohane 2:6). Moyo wa chiyero ndi lamulo la Malemba,

---

[8] Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

[9] Pa zambiri zokhudza utumiki mu zauzimu, onani Mutu 21: "Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu."

[10] Zambiri za izi, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

ndipo ichi ndi chizolowezi choona cha okhulupirira a Chipentekoste (1 Petro 1:16). Monga mutu woti *Mkhristu* ukuyankhulira, otsatira a Khristu ayenera kuyesetsa kukhala monga Iye. Akuyenera kukhala oyera chifukwa Mulungu amene iwo amamuimirira ndi woyera. Paulo adalimbikitsa a Khristu a ku Afilipi kuti, "akhale opanda chilema komanso oyera, ana a Mulungu opanda chifukwa mu mbadwo uno wokhotakhota ndi wopotoka" (Afilipi 2:15).

Choncho muyenera kuwaonetsera anthu anu m'mene angakhalire moyo wa chikhristu. Kuti izi zitheke, mukuyenera kuphunzitsa ndi kulalikira kawirikawiri zakufunikira koti Mkhristu akhale moyo wa chiyero komanso wangwiro. Muyenera kuwaonetseranso anthu m'mene moyo woterowo umaonekera. Paulo adakumbutsa okhulupirira a mu Afilipi, "Inu ndinu mboni, Mulungunso, kuti tinakhala oyera mtima ndi olungama ndi osalakwa kwa inu akukhulupirira" (1 Atesalonika 2:10). Ndipo anawalimbikitsanso okhulupirira, "Khalani onditsanza ine, monga inenso nditsanza Khristu" (1 Akorinto 11:1). Muzitha kumanena mau omwewo kwa mamembala a mpingo wanu.

Chipentekoste chenicheni singachepetsedwe nkukhala m'thumba lazikhulupiriro za chipembedzo, ngakhale zikhulupiriro za chipembedzozo zitakhala zoona. Pa tsinde lake, Chipentekoste ndi moyo umene umafunitsitsa kusandulika ku moyo ndi ntchito za okhulupirira oyamba a zaka zana zoyamba monga zafotokozedwa m'buku la Machitidwe ndi zolemba za atumwi. Mbusa ali yense wa Chipentekoste, ayenera kotero kulunjika kukutsogolera mpingo wake ku moyo ndi ntchito za Chipentekoste chenicheni.

~ Mutu 12 ~

Amayamikira Cholowa cha Chipentekoste

Leila McKinney anali mtumwi woyambirira wa Chipentekoste kwa ana a mu Afirika. Iyeyu anadzazidwa ndi Mzimu m'masiku oyambirira a Chitsitsimutso cha ku Azuza Street ku Los Angeles, California, Amerika, kuchokera 1906 mpaka 1908. Changu cha utumwi chinadzaza chitsitsimutsocho, ndipo a Leila, pamodzi ndi azakhali awo, a Julia Hucthins ndi ena, anasunthika zopita ku Afirika kukalalikira uthenga wabwino. Leila adalemba mu nyuzipepala ya *Apostolic Faith*, "Ndine wokonzeka kumkhulupirira Iye kupita ku Afirika. Ndikudziwa Ambuye afuna kuti Ine ndipite kumeneko. Ndifuna ndikachitire umboni kwa anthu ndi kukaphunzitsa ana za Ambuye wodala, ndikuti agwire ntchito ya Ambuye. Ndine wokonzeka kusiya okondedwa anga onse chifukwa cha Iye." Nkhani ya Leila McKinney ndi imodzi mwa nkhani miyandamiyanda zokhudza Chitsitsimutso cha Chipentekoste mu Afirika.

Ndi zofunikira kwambiri kuti mbusa wa Chipentekoste muAfirika azindikire ndi kuyamikira m'mene uthenga wa Chipentekoste unabwerera ku dziko la Afirika. Mbusa wina wa Chikuda adanenapo, "Ngati sitikudziwa kumene tinachokera, ndiye kuti sitikudziwa chomwe tili, kapenanso komwe tikupita." Pamene sitikumvetsetsa kale lathu, tifanana ndi bwato losayenda. Timakhala pangozi yakuyendayenda wopanda chitsogozo chomveka bwino komanso opanda

cholinga. Koma tikadziwa kumene tinachokera ndi chifukwa chimene tikupezekera panopa, timayenda molimba mtima kupita kutsogolo.

Mutu uwu udzayankha mafunso angapo ofunikira, zokhudza mayambidwe a Chipentekoste mu Afirika: Kodi Chipentekoste cha masiku anochi chiyambi chake chinali chotani? Ndi liti, ndipo chinabwera bwanji ku Afirika? Chipentekoste chinafalikira motani mu Afirika? Ndi zobetchera zotani zimene mpingo wa Chipentekoste mu Afirika ukumana nazo lero? Tsogolo la Chipentekoste mu Afirika ndi lotani?

CHIYAMBI CHAKE

Kumapeto a mwezi wa Disembala m'chaka cha 1900, pa Baibulo Sukulu yaing'ono mu Topeka, Kansas, Amerika, Charles Fox Parham adapereka ntchito yakafukufuku kwa ophunzira ake. Adawauza kuti afufuze m'Malemba ndikupeza "Umboni wa Baibulo" wokhudza ubatizo wa Mzimu Woyera. Patapita nthawi yakusanthula mwakathithi, ophunzira adakapereka zomwe adazipeza kwa Parham. Iwo adawombera mkota kuti, umboni wa Baibulo wa Mzimu unali kulankhula ndi malilime monga Mzimu amalankhulitsa.

Kenako iwo anayamba msonkhano wa pemphero umene unapitirira kwa masiku angapo. Mosakhalitsa, nthawi itadutsapo pakati pa usiku, pa 1 Januwale 1901, Mzimu Woyera anadza mwa mphamvu pa mkazi dzina lake Agnesi Ozman. Modabwitsa, adayamba kulankhula m'malilime monga Mzimu adamulankhulitsa. Mkatikati mwa masiku, ambiri enanso kuphatikizapo Parham adabatizidwa mwa Mzimu Woyera, ndi chitsimikizo cholankhula ndi malilime. Monga zotsatira za kudzazidwa ndi Mzimu, Parham ndi ophunzira ake adayamba kulalikira uthenga wabwino ndi mphamvu yaikulu ndi ulamuliro, mofanananso ndi okhulupirira a mbuku la Machitidwe. Mitima yawo inagwidwa ndi changu chachikulu cha utumwi. Parham adakhulupirira kuti Mulungu amatsanulira Mzimu Wake kuti apereke mphamvu ku mpingo kuti ukafikire mafuko ndi uthenga wabwino wa Khristu asanabwerenso Iye posachedwapa

Mu 1905, Parham adasamutsira sukulu yake ku Houston, Texas, Amerika, kumene adapitiriza kuphunzitsa za ubatizo mwa Mzimu Woyera. Posakhalitsa, Lucy Farrow adalowa nawo bungweli. Kenako Iyeyu adamusonyeza Parham kwa William J. Seymour, mlaliki wa Chikuda wa ku Amerika wa chiyero. Seymour adamvetsera kwa Parham akuphunzitsa, ndipo iyenso adavomereza uthenga wa Chipentekoste.

Mu nthawi yochepa, Seymour adalandira maitanidwe kuchokera ku mpingo wina waung'ono wa Holinesi mu Los Angeles. Mu uthenga wake woyamba m'mpingo umenewu, Iye analalikira uthenga wa ubatizo mwa Mzimu Woyera ndi chitsimikizo cholankhula m'malilime. Mbusa Julia Hutchins, adaukana uthengawo ndipo adamukaniza Seymour kukhala gawo limodzi la utumiki wapamalopo.

Seymour kenako adayamba kulalikira uthenga wa Chipentekoste mu nyumba za mamembala a mpingo. Pamene amalalikira, ndipo anthu mkupemphera, ambiri amadzazidwa ndi Mzimu. Gulu la anthu lidachuluka koposa kotero kuti adakakamizidwa zogula tchalitchi chakale ku Msewu wa Azusa. Mulungu adapitiriza kutsanula Mzimu Wake, ndipo kwa zaka zitatu, kuchokera 1906 mpaka1908, anthu zikwizikwi adabwera kuchokera dziko lonse lapansi ndipo adadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Adabwerera ku nyumba zawo ndi uthenga woti, Chipentekoste chafika.

Kuchokera ku Msewu wa Azusa, atumwi a Chipentekoste adapita ku maiko oposa khumi ndi asanu mu zaka ziwiri, kuphatikizapo China, India, Japan, Egypt, Liberia, Angola, ndi South Afirika. Chitsitsimutso chachikulu cha ku Msewu wa Azusa chidachita kwakukulu kufalitsa Chipentekoste pa dziko lapansi, kuposa china chili chonse. Lero pali mipingo yokwanira makumi awiri ndi zisanu ndi chimodzi (26) ya Chipentekoste imene mayambidwe awo amalumikizika ku Msewu wa Azusa, kuphatikizapo Assemblies of God.[1]

Mu zaka zomwezo Mulungu amatsanuliranso Mzimu Wake m'madera ena kudziko lapansi. Malo ena amene adali oyambirira a Chitsitsimutso cha Chipentekoste anali ku Wales (1901), India (1905), England (1907), Korea (1907), Chile (1909), ndi malo enanso. Mulungu anakwaniritsa lonjezano limene adalonjeza kwa Yoweri mneneri: "M'masiku otsiriza, atero Mulungu, ndidzatsanulira Mzimu wanga pa anthu onse" (Machitidwe 2:17: fanizila Yowele 2:28).

[1] Pa zambiri zammene Chitsitsimutso chaku Azusa chinakhudzira Afirika, onani buku lolembedwa ndi Denzil R. Miller, *Kuchokera ku Azusa kupita ku Afirika ku Maiko*, likupezeka mwaulere pa www.DecadeofPentecost.org.

CHIPENTEKOSTE CHAFIKA MU AFIRIKA

Tsopano, tiyeni tione m'mene uthenga wa Chipentekoste unafikira ku Afirika ndi m'mene unafalikira mu dziko lonse la Afirika.

Chipentekoste Chifika ku Afirika

Atumwi oyambirira a Chipentekoste kuchokera ku Amerika kupita ku Afirika adabwera kuchokera ku Mishoni yaku Msewu waku Azusa kwenikweniko. Adafika mu Liberia mu chaka cha 1907. Gulu lawo mudalinso Lucy Farrow, J. W. ndi Julia Hutchins, mdzukulu wa Leila McKinney, ndipo kwa kanthawi chaka chomwecho adafikaso a Edward McCauley. Anthu okwana khumi ndi awiri, amuna ndi akazi a Chikuda a ku Amerika, ndi ana ochokera ku Msewu wa Azusa adapita ku Liberia mchaka chimenecho m'magulu awiri. Mkati mwa masabata, asanu ndi awiri a iwo adamwalira ndi malungo kapena matenda ofananiranako ndi malungo. Komabe anaona anthu a ku Liberia ambiri akubwera kwa Ambuye ndi kubatizidwa mwa Mzimu Woyera. Mpingo woyamba wa Chipentekoste wokhazikika mu Afirika unadzalidwa mu Monrovia mu 1907. Atumwi ochokera ku Msewu wa Azusa adapitanso ku South Afirika ndi Angola.

Mulungu anagwiritsanso ntchito eni nthaka a Chifirika kufalitsa uthenga wa Chipentekoste. Nkhani ziwiri zokhazikika ndi za Eliya Letwaba aku South Afirika ndi a William Wade Harris aku Liberia. Amuna amenewa anathandizira kukhazikitsa mabungwe omwe anathandizira kukhudza maiko angapo a Kumwera ndi Kuzambwe kwa Afirika, zomwe zinapangitsa anthu zikwizikwi kuti abwere kwa Khristu.

Elias Letwaba (1870-1959) anatchulidwa kuti anali Mlaliki Wachikuda wa Chipentekoste wamphamvu kwambiri mu mbiri ya South Africa. Mu chaka cha m'ma 1870, pamene Eliya anali akanali m'mimba ya amayi ake, mayiyo analandira masomphenya kuchokera kwa Mulungu. Mzimu adamuuza kuti mwana wake tsiku lina Mulungu adzamugwiritsa ntchito monga chida Chake kuti akakhazikitse mipingo. Letwaba anakula ali ndi njala yayikulu yofuna kumdziwa Mulungu ndi kugwiritsidwa ntchito ndi Iye.

Mu 1908, adakumana ndi John Lake, mtumwi wa ku Amerika amene asanabwere ku South Afirika, adalandila Mzimu Woyera pansi pa utumiki wa Charles Parham. Lake adalinso atakhalapopachitsitsimutso cha ku Msewu wa Azusa mu Los Angeles. Letwaba ndi Lake adayenda pamodzi mu utumiki mpaka 1913, pamene Lake adabwerera ku Amerika.

Monga momwe Mulungu adamuonetsera mai ake a Letwaba, a Elias adakhaladi mlaliki wamphamvu wa Chipentekoste, komanso mphunzitsi amene adatsogolera ambiri ku chipulumutso komanso ku ubatizo wa Mzimu Woyera. Adaona zikwi za anthu akuchiritsidwa, komanso zikwi za anthu akupulumutsidwa mu South Africa komanso ku Rhodesia (Zimbabwe). A Letwaba adali a Apostolic Faith Mission ku South Afirika. Iwowa adayambitsa Patmosi Baibulo Sukulu, sukulu yoyamba mu South Africa kuyendetsedwa ndi munthu wakuda. A Letwaba adalalikira mosatopa mpaka imfa yawo mu 1959.

William Wadé Harris (c. 1860-1929) adagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kufalitsa uthenga wabwino ku madzulo kwa Afirika. Iyeyu amatchulidwa kuti "Mlaliki wopambana kwambiri mu Afirika." Mu zaka zoyambirira atakula, adali wa Mipingo ya Chi Methodist ndi Episipoko mu Liberia. Iye adakhala mu Monrovia pa nthawi imene atumwi ochokera ku Msewu wa Azusa adalinso komweko. Ena amakhulupirira kuti atumwi amenewa a Chikuda aku Amerika ndiwo adali gwero la Maganizidwe a Chipentekoste a Harris.

Harris adachitira umboni kuti, mngelo, Gabrieli, adawonekera kwa iye mu m'masomphenya namuuza kuti ambiri adzabwera kwa Khristu kupyolera mu utumiki wake wa uneneri. Potsatira masomphenya amenewo, Harris adayenda kuzungulira Liberia, Coted'Ivoire, Ghana, ndi Sierra Leone, akuuza anthu kuti asiye machimo awo ndi kutembenukira kwa Khristu. Adatumikira mu mphamvu ya Mzimu, kutululutsa ziwanda, kuchilitsa odwala, komanso kulankhula m'malilime. Komanso adanenetsa kuti anthu asiyezamafano zawo, akhulupirire mwa Yesu, ndipo adikire azungu kuti abwere ndi mabaibulo kuti adzawaphunzitse Mau a Mulungu. Zimaganizilidwa kuti anthu oposa zana limodzi adatembenuka mtima kupyolera mu utumiki wake.

Letwaba ndi Harris ndi zitsanzo ziwiri za zikwizikwi za abusa a Chikuda, alaliki, aphunzitsi, komanso atumwi amene alalikira uthenga wabwino wokwanira mu Afirika, kulengeza kuti Yesu amapulumutsa, amachiritsa, amabatiza mwa Mzimu Woyera,komanso akubwera posachedwa.

Chipentekoste Chifalikira ku Afirika

Nkhani ya kufalikira kwa Chipentekoste ku Afirika kudzera mu Assemblies of God (AG), ndi mbiri ya Mzimu wogwira ntchito kudzera mwa atumwi ochokera kumaiko achizungu ndi atumwi a Chikuda kudzala mpingo mu Afirika. Pamene Assemblies of God ndi mpingo umodzi mwa mipingo yochuluka ya Chipentekoste

mu dziko la Afirika, Mulungu wagwiritsa ntchito bungwe limeneli mwamphamvu kufalitsa uthenga wabwino wa Khristu. Tiyeni tione ziwiri mwa nkhani zotero.

Liberia. Mu 1908, Jasper Klabioh Toe adapemphera, "Ngati kuli Mulungu Mlengi, ndithandizeni kuti ndimpeze Iye." Mulungu adalankhula ndi Toe, namuza kuti, "Yenda kupita kunyanja yayikulu." Panthawi yomweyo Mzimu adakhala akuchita ndi mtumwi wa ku Amerika, John Moore Perkins. Perkins adabatizidwa mwa Mzimu Woyera pamene adakhala nawo pa msonkhano wa chitsitsimutso wa Chipentekoste ku Toronto, Canada. Kenako, Mulungu adamulamulira zopita ndi uthenga wa Khristu ku Liberia.

Pamene anali pa Nyanja kudutsa pagombe la Liberia, Perkins adamva Mzimu akumuuza iye kuti apite cha pamtunda pamalo penapake. Oyendetsa sitima adamuchenjeza, "Ano si malo otetezedwa." Perkins, komabe adaumilira kuima. Iye ndi gulu lake adatsika pamalo penipenipo pamene Mzimu adamutsogolera Toe. Linali tsiku la Khirisimasi mu chaka cha 1908. Perkins adagawa uthenga wabwino kwa Toe, amene mwa changu adalandira Khristu. Ntchito imene Toe ndi Perkins adayiyamba idakula nkukhala Liberia Assemblies of God. Lero mpingowu ndiwo waukulu kwambiri wa Chipentekoste mu dzikolo.

Nigeria. Mu mayambiriro a zaka za 1930, Augustine Ehurieiwe Wogu waku Port-Harcourt, Nigeria, adapeza magazini yotchedwa Pentekoste Evangeli, yosindikizidwa ndi Assemblies of God ku Amerika. Wogu adakopedwa ndi zomwe adawerenga mu magazini zokhudza machiritso a uzimu ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Zotsatira zake, anayamba kupempherera odwala ndi kuwatsogolera ku ubatizo wa Mzimu. Pamene mpingo umene amapempherako udakana ziphunzitso zake za Chipentekoste, Wogu ndi ena ochepa anachoka nakayambitsa mpingo Woima pawokha wa Chipentekoste umene adautchula kuti Mpingo wa Yesu Khristu.

Patapita zaka zingapo, mu 1939, Wogu adakumanizana ndi atumwi aku Amerika mu Port-Harcourt. Adabwera ku Nigeria kudzafufuza kuthekera koti Assemblies of God idzayambitse ntchito kumeneko. Wogu adawapempha iwo kuti atumize atumwi oti adzamuthandize. Ku Mishoni adavomera ndipo adatumiza gulu lotsogozedwa ndi W. Llyod Shirer kuti akagwire ntchito ndi Wogu. Iwo adagwirizana zoutchula mpingowu kuti Assemblies of God Nigeria. Lero, mpingowu ndiwaukulu kwambiri pamipingo ya Assemblies of God mu Afirika. Assemblies of God Nigeria, ili ndi mamembala oposera miyanda itatu (3 million).

Izi ndi zitsanzo ziwiri chabe za mazana mazana a nkhani zomwe zingathe kukambidwa. Zimenezi, komabe, zimapereka mbiri ya m'mene Mzimu wa Mulungu anasesera Afirika kudzera mu mgwirizano wa anthu Akuda ndi iwo amene Mzimu adawatuma ku Afirika. Nkhani zinanso zikhozanso kukambidwa za m'mene lawi la Chipentekoste lidayatsira ziyanjano za m'mpingo ina mu dziko la Afirika, monga The Church of Pentecost ku Ghana, komanso The Full Gospel Believers' Church ku Ethiopia.

Africa Assemblies of God. Pamene uthenga wa Chipentekoste udabwera koyamba ku Liberia, mu 1906, kunalibe mipingo ya Chipentekoste kapena okhulupirira kwina konse mu Afirika. Koma Mulungu, anali akuyamba kutsanulira Mzimu pa dziko la Afirika. Kukula kwa Assemblies of God, ndi chitsanzo chochititsa kaso cha m'mene Mulungu wadalitsira Afirika. Pofika 1948, mpingo waAssemblies of God mu Afirika, udali utakula kufika pa okhulupirira zikwi makumi awiri (40,000), osonkhana mu ma tchalitchi okwana mazana asanu ndi awiri (700), m'maiko khumi ndi limodzi (11).

Mu chaka cha 1989, Assemblies of God idapanga mgwirizano wotchedwa Africa Assemblies of God Alliance (AAGA), wokhala ndi mipingo ya mmaiko mu dziko la Afirika. Chaka chinacho, AAGA idakhazikitsa zaka zotchedwa "Zaka Khumi za Kholola," zopitilira kuchokera 1991 mpaka 2000. Kutsindika kunali pa kudzala mipingo ndi utumwi mu mphamvu ya Mzimu. Mu zaka khumi zimenezo mpingo unakula kuchoka mamembala miyanda iwiri ndi zana limodzi (2.1million) osankhana mu m'matchalitchi okwana zikwi khumi nchimodzi, mazana asanu nlimodzi, mphambu makumi asanu nzitatu (11,688) m'maiko makumi atatu ndi chimodzi (31), kufika pa mamembala okwana miyanda isanu ndi umodzi, mazana atatu (6.3 million) osonkhana m'matchalitchi okwana zikwi makumi awiri ndi zinai, ndi mphambu khumi nzisanu ndi zinayi (24,019), m'maiko okwana makumi atatu ndi limodzi (31). Chilimbikitso chomwe chinapezeka mu zaka Khumi za Kholola chinapitirira kufika mu zaka zina khumi. Pofika 2010, Africa Assemblies of God idali itakula kufika pa mamembala okwana miyanda khumi ndi isanu ndi umodzi, mazana asanu ndi limodzi (16.6 million), osonkhana m'mtchalitchi okwana zikwi makumi asanu nchimodzi, zisanu nziwiri, mazana asanu ndi atatu, mphambu makumi awiri, zisanu nziwiri (67,827).

Mu Januwale 2010, AAGA idakhazikitsa zaka zinanso khumi, zotchedwa "Zaka Khumi za Pentekoste" (2010-2020). Cholinga choonjezerapo chinali kuona mamembala okwana miyanda khumi (10 million) akubatizidwa mwa Mzimu

Woyera ndi kumemedwakukhala mboni zopatsidwa mphamvu ndi Mzimu. Pamapeto pa 2019, Africa Assemblies of God idakula kufika pa mamembala okwana miyanda khumi ndi itatu, mazana asanu ndi awiri (18.7 million) osonkhana m'matchalitchi okwana zikwi makumi asanu nzitatu, zisanu nziwiri, mazana asanu ndi awiri, mphambu makumi anai ndi imodzi (87,741) Kum'mwera kwa Sahara ku Afirika ndi ku chidikha cha Nyanja ya Mchere ya India.

Mu mwezi wa Januwale 2021, AAGA idakhazikitsa zaka khumi zina kachitatu ndi kutsindika kotchedwa "Zaka Khumi zaChitsitsimutso." Mu zaka khumi zimenezi, mpingo udzapitiriza kutsindika kwake pa kufalitsa uthenga, Ubatizo wa Mzimu, kudzala mipingo, ndi utumwi. Chimodzi mwa kutsindika kwa Zaka Khumi za Chitsitsimutso ndi chakuti, Africa Assemblies of God ikuyang'ana ku Mpoto kwa Afirika, ndi cholinga chokhazikitsa ma bungwe odzala mipingo mu mphamvu ya Mzimu kudera kumene mmbuyomu kudasiyidwa.

KUKHUDZA KWA CHIPENTEKOSTE

Chipentekoste chasintha nkhope ya mpingo wa mu Afirika mu njira zambiri. Kukula kwa mpingowu kwakhala kotamandika. Mu 2015, kafukufuka wa Oxford Research Encyclopedia adafotokoza kuti panali a Chipentekoste okwana miyanda mazana awiri ndi iwiri (202 million), (atsitsimuli) mu Afirika, kupanga magawo okwana makumi atatu ndi asanu a zana (35%) ya chiwerengero chonse cha Akhristu ndi magawo khumi zisanu nziwiri a zana (17%) a chiwerengero chonse. Mu milingo yosiyana, moonekeratu mpingo uli wonse wa Chifirika wakhudzidwa. Mipingo yambiri ya miyambo ya mokolo atengerako machitachita owonetsera a Chipentekoste monga kuyimba ndi chimwemwe, kulambila momasuka, ndi pemphero lokangalika. Angapo atengera zina mwa zizolowezi za a Chipentekoste monga, kubadwa mwatsopano, kulankhula m'malilime, ndi utumiki wa mphamvu.

Chikhristu cha Chipentekoste chakhudzanso chikhalidwe cha Afirika kwakukulu. Njira imodzi apangira izi, ndikudzera mu choonekera chotchedwa "chiombolo ndi kutukula." Pamene asanduka a Khristu odzipereka, miyoyo yawo imasintha, ndipo "amatukulidwa" kuchoka m'machimo awo ndi chionongeko. Zotsatira zake, amasanduka anthu abwino komanso mbeu yopindulitsa. Komanso, akhristu odzipereka kawirikawiri amalondola maphunziro a pamwamba, amalimbikira ntchito, amapeza ntchito zabwino, ndipo amafuna kuchita ungwiro pa chuma. Kawirikawiri amatambasula manja ku zachifundo, kusamalira ovutika m'moyo. Kuonjezera apo, Akhristu ena a Chipentekoste, akutengera zikhalidwe

zawo ku dera la ndale ndipo akupanga kusintha kumeneko. Ntchito zotere ndi zina zapangitsa kukhala ndi dziko labwino. Pamene si a Khristu onse a Chipentekoste amakhala moyo woonetsera Khristu mu dziko, iwo amene akuyesetsa kutero akupanga kukhudza kwabwino.

KUYANG'ANA TSOGOLO

Mpingo wa Chipentekoste wa lero mu Afirika wayima pa mphambano. Pamene ukulingalira za kale lake, utha kudzitamandira pazigonjetso zambiri, monga takambilana mu mutu uwu. Komano pamene Chipentekoste cha Afirika chikuyang'ana kutsogolo, chikukumana ndi zokhoma zambiri. Zitatu mwa zokhoma zimenezi ndi, chiopsezo cha kupotoka kwa chiphunzitso, kupinimbidzira kwa uzimu, komanso kudzikonda.

Pochitapo kanthu, inu monga mbusa wa Chipentekoste, mudzachita bwino mutadzifunsa nokha mafunso ofufuza awa:

- Kodi ndidzakhalabe woona ku Malemba, kapena ndidzatsogolera mpingo wanga ku chiphunzitso cholakwika?
- Kodi ndidzatsogolera mpingo wanga mu Chitsitsimutso chenicheni cha Chipentekoste, kapena ndidzalola kuti ulowe "nkupinimbidzira kwa uzimu," "wokhala nawo maonekedwe a umulungu koma mphamvu yake kuikana" (2 Timoteo 3:5).
- Kodi ndidzatsogolera anthu anga kukafuna otaika mu mphamvu ya Mzimu Woyera, kapena ndidzawatsogolera kulondola zachabe, ndi zodzikonda za chuma ndi mdalitso wawekha?

Tsogolo la mpingo wa Chipentekoste mu Afirika kwakulu likudalira m'mene inuyo ndi zikwizikwi za abusa ena a Chipentekoste angayankhire mafunso amenewa.

Ngati abusa a Chipentekoste mu dziko la Afirika atadzipereka ndi mtima wonse kukhala owona ku cholowa chawo cha Chipentekoste, ndi kukhala wa Chipentekoste weniweni mu chiphunzitso, mu moyo, komanso mu ntchito, tsogolo ndi lowala. Koma akapanga chisankho chosiya cholowa chawo ndi kukhala monga ena owazungulira, tsogolo la Chipentekoste mu Afirika layima mu chiopsezo. Ndizofunika kwambiri, choncho, kuti abusa a Chipentekoste mu Afirika ndi chidwi alondole zitsanzo za umulungu za makolo awo.

Cholowa ichi cha Chipentekoste ndi kudaliridwa kopatulika. Chitsisimutso chenicheni cha Chipentekoste ndicho chiyembekezo chomaliza cha dziko lapansi.

Ngati mphatso ya Pentekoste ingasungidwe ndi kukolezedwa, ingathe kuphulika nkukhala lawi loyaka, kufalikira kuchokera ku Afirika kupita ku mafuko a dziko lapansi. Koma, ngati italekereredwa ndi kunyozedwa, ikhoza kuzilala ndi kufa. Abusa a Chipentekoste mu Afirika momwemo ayenera kumvera mau a Paulo kwa Timoteo, mtumiki mzake wa chichepere wa Chipentekoste komanso mbusa wa mpingo wa mu Efeso: "Ndikukumbutsa iwe kuti ukoleze mphatso ya Mulungu, imene ili mwa iwe mwa kuika manja kwanga" (2 Timoteo 1:5). Paulo adaonjezapo, "Chosungitsa chokomacho udikire mwa Mzimu Woyera amene akhalitsa mwa ife" (v.14).

Monga abusa a Chipentekoste mu Afirika, ifenso tiyenera kusunga ndi kukoleza mphatso ya Mulungu imene yapatsidwa kwa ife ndi onyamula Chipentekoste makolo athu. Ndipo monga iwo, tiyenera kusunga mokhulupirika ichi chomwe chapatsidwa kwa ife mwa Mzimu Woyera amene akhala mwa ife natipatsa ife mphamvu.

~ Gawo 4 ~

MOYO WA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

~ Mutu 13 ~

Moyo Wosamalidwa Bwino

Mbusa wachinyamatayo anakhala polembera pake mutu wake ataukwirira m'manja mwake. Zofuna za utumiki mu ubusa zinali kukhala zochuluka kuposa momwe iye akanatha kupirira. Iye ankaganiza zosiya utumiki n'kuyambiranso ntchito. Komabe, chimene Mbusa wachinyamatayu sanazindikire n'chakuti sanali yekha m'mavuto akewa. Mu Afirika monse, abusa ochuluka a Chipentekoste akupezeka m'makhalidwe ofana. Amaona kuti sangapitirizebe kulimbana ndi zopsinja zambiri za utumiki.

Chifukwa chimodzi chimene abusawa amadera nkhawa kwambiri n'chakuti sanaphunzire kuyendetsa bwino moyo wawo. Amakhala moyo wosasamalidwa bwino moti vuto lililonse limene akumana nalo limawadzidzimutsa, n'kuwasokoneza.

Ngakhale kuti n'kosatheka kuti Mbusa wa Chipentekoste aganize kuti angathe kuthawa zipsinjo zonse za moyo ndi utumiki, sikuli kosatheka kuti akhulupirire kuti angathe kuthana ndi mavuto amenewa. Mutu uwu upereka upangiri wa momwe inu, monga Mbusa wa Pentekoste, mungakwaniritsire moyo woyendetsedwa bwino.

KUFUNIKA KWA MOYO WOSAMALIDWA BWINO

Dzina limodzi la m'Baibulo la Mbusa ndi woyang'anira (1Tim. 3:1-2). Paulo analangiza akulu a ku Aefeso kuti: "Tadzichenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira kuti muwete Mpingo wa Mulungu" (Mach. 20:28). Monga oyang'anira, Mbusa "amasamalira banja la Mulungu" (Tito 1:7). Choncho Mbusa wa Chipentekoste ali ndi udindo woyendetsa bwino nkhani za mpingo wapamalo. Komabe, asanayendetse bwino tchalitchi, choyamba ayenera kukhala okhoza kuyendetsa bwino moyo wake.

Moyo Wosamalidwa Bwino

Ngakhale kuti moyo wosamalidwa bwino sukhala wopanda nkhawa, komanso suli wodzaza ndi chisokonezo komansochibalaliko. Moyo wosamalidwa bwino udzakupatsani chidaliro chomwe mukufunikira kuti mupite patsogolo mu utumiki.Zidzakuthandizani kuti mukhale opindulitsa—kuchita zambiri ndi khama lochepa. Ndipo zidzakuthandizani kuthana ndi zovuta za moyo. Tiyeni tiwone mbali zinayi za moyo woyendetsedwa bwino:

1. Cholinga. Moyo woyendetsedwa bwino ndi moyo wokhala ndi cholinga chomveka. Paulo anatchula cholinga cha Mulungukukhala "chifuniro cha Mulungu chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro" (Aroma 12:2). Mukamvetsetsa bwino lomwe cholinga cha Mulungu pa moyo wanu, m'pamenenso mudzakhala wogwira mtima kwambiri pokonza moyo wanu mogwirizana ndi cholinga chimenecho.

Kunena mwachidule, inu, ngati Mbusa wa Chipentekoste-monga wotsatira wina aliyense wa Khristu—mumakhala ndi moyo kulemekeza Mulungu ndi kuchita chifuniro chake. Ngakhale mungavomereze chowonadi ichi, musayimire pomwepa. Muyenera kuyesetsa kudziŵa chifuniro cha Mulungu changwiro, kapena chokwanira, pa moyo wanu. Muyenera kudziwa chifukwa chake Mulungu wakuyikani mu mpingo wanu panthawiyi. Muyenera kufunafuna Mulungu m'pemphero ndi kumufunsa kuti, "Ambuye, mwanditengeranji kumalo ano?" ndikuti "Kodi mukufuna kuti ndikwaniritse chiyani ku ulemerero Wanu?"

2. Zinthu zofunika. Mutamvetsetsa bwino lomwe cholinga cha Mulungu pakukhala kwanu mu mpingo wanu panthawiyi, mutha kuyamba kupanga zoyambirira zanu zaumwini ndi zautumiki. Zomwe mumayika patsogolo ndi zomwe mumaziona kuti ndizofunikira kwambiri. Ndizinthu zomwe mumaikilako chidwi kwambiri poikapo nthawi yanu komanso mphamvu zanu. Khristu

analankhula za zinthu zofunika kwambiri m'moyo wake pamene anati, "Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndichite chifuniro changa, koma chifuniro cha Iye amene anandituma Ine" (Yohane 6:38).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, mutha kugwiritsa ntchito kumvetsetsa kwanu kwa chifuniro cha Mulungu kukutsogolerani popanga utumiki wanu ndi zisankho za moyo wanu. Mutha kufunsa chilichonse chomwe mungachite kuti, "Kodi ntchitoyi ikundithandiza bwanji kukwaniritsa cholinga cha Mulungu pa moyo wanga?" Ntchito iliyonse imene imapititsa patsogolo chifuno cha Mulungu iyenera kulandiridwa. Ntchito iliyonse imene sikupititsa patsogolo chifuno cha Mulungu iyenera kupewedwa kapena kusiyidwa.[1]

3. Kuchita zinthu mokhazikika. Kuonjezarapo, moyo woyendetsedwa bwino ndi moyo wokhazikika. Moyo wokhazikika ndi umene umalinganiza nthaŵi ndi mphamvu zoyenera kuchita chilichonse chofunika m'moyo. Munthu amene akufuna kuwoloka mtsinje pa tsinde la mtengo umene wagwa ayenera kusamala. Ngati atsamira kutali kwambiri kudzanja lamanzere kapena lamanja, adzagwera m'madzi. Chimodzimodzinso ndi Mbusa wa Chipentekoste. Ngati chindunji cha maganizo awo onse aika pa mbali imodzi kapena ziwiri za moyo kapena utumiki, iwo ali chiopsezo chakutaika ndi kulephera pa mbali ina yofunika kwambiri.

Mwachitsanzo, inu monga Mbusa mukhoza kuthera nthawi yambiri mukusamalira anthu a m'tchalitchi mwanu mpaka kunyalanyaza banja lanu. Kapena mungakhale odzipereka pakukonzekera ulaliki kotero kuti mumanyalanyaza pemphero kapena kufikira otayika. Monga Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste, muyenera kuyesetsakukhala okhazikika m'mbali zosiyanasiyana za moyo, monga

- kulinganiza pakati pa zochita ndi umunthu wanu;
- Kugwirizana pakati pa ntchito ndi kupuma;
- mgwirizano pakati pa utumiki ndi banja;
- kukhala ndi malire pakati pa kusamalira ena ndi kudzisamalira,

Mawu a Yesu kwa Afarisi amagwiranso ntchito pano. Anawatsutsa ponena za kulimbikira kwawo kupereka chachikhumi, kwinaku akunyalanyaza miyambo ina

[1]Kuti mudziwe zambiri pa zomwe mbusa wa Chipentekoste amaika patsogolo pa umunthu wake ndi utumiki wake, onani Mutu 4: "Munthu Amene Wakonzekera Bwino," ndi Mutu 5: "Zofunikira Zoyambirira za Utumiki."

yofunika kwambiri. Iye anati: “Bwenzi mutachita izi, ndi kusasiya zinazo” (Luka 11:42)

4. Chitsogozo. Pomaliza, kwa Mbusa wa Chipentekoste, moyo woyendetsedwa bwino ndi moyo wotsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Pamene mutsatira kwambiri chitsogozo cha Mzimu Woyera, moyo wanu udzakhala wadongosolo.

Paulo analimbikitsa okhulupirira a ku Galatiya kuti: “Muyendeyende ndi Mzimu, ndipo musafitse chilakolako cha thupi” (Agal. 5:16) Paulo analimbikitsa okhulupirira a ku Galatiya. Kenako anandandalika “zilakolako za thupi” zingapo. Taonani mmene chilichonse cha zimenezi chingatchulidwe kukhala chipatso cha moyo wosasamalidwa bwino kapena wosachita mwambo: “dama, chodetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga, madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mchezo, ndi zina zotere” (Agal. 5:19-21).

Inde kumbali ina, kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera ndiko kukhala moyo wodzipereka kwa Mulungu. Moyo woterowo umafuna kukulitsa “chipatso cha Mzimu.” Paulo akudzindikira chipatso chimenechi kuti ndi “chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso” (Agal. 5:22-23). Taonani mmene ukoma uliwonse ungatchulidwe kukhala khalidwe la moyo wosamalidwa bwino. Umapangidwa ndikukhala mwa Khristu (Yohane 15:5) ndi kuyenda mu Mzimu (Agal. 5:24-25).

Chitsanzo Chathu cha Moyo Wosamalidwa Bwino

Yesu ndiye chitsanzo chathu changwiro cha munthu amene amakhala moyo wosamalidwa bwino. Yesu analamulira moyo wake motsatira ndondomeko ya Atate wake, ndipo anayenda mogwirizana ndi dongosolo la Atate wake. Chifukwa cha zimenezi, anatha kukhazikika pa ntchito yake. Taonani mmene moyo wa Yesu umaperekera chitsanzo cha makhalidwe anayi otchulidwa pamwambawa a moyo wosamalidwa bwino:

- *Cholinga*. Yesu ankadziwa cholinga chake pobwera, ndipo anakhalabe wokhulupirika ku ntchito ya moyo wake. N’chifukwa chake pamene utumiki wake unalikumapeto, anatha kupemphera kwa Atate wake kuti: “Ine ndalemekeza Inu padziko lapansi, m’mene ndinatsiriza ntchito imene munandipatsa kuti ndichite” (Yohane 17:4).

- *Zinthu zofunika.* Nthawi zonse Yesu ankaika zinthu zofunika patsogolo. Mwachitsanzo, iye anaika patsogolo kukhala pa ubwenzi wolimba ndi Atate wake. Marko analemba za Iye kuti: "Ndipo m'mawa mwake anauka usikusiku, natuluka namuka kuchipululu, napemphera kumeneko" (Marko1:35).
- *Kuchita zinthu mokhazikika.* Yesu ankakhala ndi moyo wabwino kwambiri. Iye mwa dongosolo labwino anali kugwira ntchito ndi kupuma (Marko 6:31-32). Chifukwa Iye ankakhala moyo wadongosolo, Iye sanali wokhumudwa kapena kuchita zinthu mwaphuma. Nthawi zonse anali pamalo abwino pa nthawi yoyenera kuchita zinthu zoyenera.
- *Chitsogozo.* Yesu anakhala moyo wake motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Iye anali wodzala ndi Mzimu (Luka 4:18-19), ndipo nthawi zonse ankachita monga momwe Mzimu unamuuzira (Mat. 4:1; Luka 4:1). Iye anati ponena za iye mwini, "Sangathe Mwana kuchita kanthu pa yekha, koma chimene aona Atate achichita, ndicho. Pakuti zimene Iyeazichita, zomwezo Mwananso azichita momwemo" (Yohane 5:19).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuchipanga kukhala cholinga chanu kutsatira chitsanzo cha Yesu (1 Yohane 2:6).

Ubwino Wamoyo Wosamalidwa Bwino

Ngakhale kuti kukhala ndi moyo wosamalidwa bwino kumafuna khama, kwa Mbusa wa Pentekoste ndi khama logwiritsidwa ntchito bwino. Mbusa amene amayendetsa bwino moyo wake adzakhala ndi zokolola zambiri mu utumiki. Chifukwa chakuti nthawi yawoimayendetsedwa bwino, amatha kuchita zambiri ndi khama lochepa.

Komanso, moyo wosamalidwa bwino umabweretsa mtendere wochuluka wamaganizo. Kuyendetsa bwino moyo kumatengera dongosolo, ndipo dongosolo limatengera mtendere. M'moyo wake wonse, Yesu anasonyeza mtendere wamumtima wachilendo. Pamene ena anachita mantha, Iye anakhala chete. Mwachitsanzo, pamene ophunzira ake anachita mantha ndi namondwe, Iye anagona mwamtendere m'ngalawa (Mateyu. 8:23-27). Zomwezinso zinachitika ndi Paulo paulendo wake wopita ku Roma (Machitidwe 27:27-38).

Moyo woyendetsedwa bwino umaonjezanso moyo wautali muutumiki. Moyo wosasamalidwa bwino umabweretsa kupsinjika, ndipo kupsinjika kumabweretsa kutopa. Koma, moyo wosamalidwa bwino umabweretsa mtendere, umene umathandiza chipiriro chokulirapo mu utumiki.

MADERA ATATU A MOYO WOSAMALIDWA BWINO

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kukwanitsa kuyendetsa bwino mbali zitatu za moyo ndi utumiki, motere:

Kusamalira Ndalama

Choyamba, muyenera kuphunzira kugwiritsa ntchito bwino ndalama zanu. Mukhoza kuyamba izi podzikumbutsa kuti zonse zomwe muli nazo ndi za Mulungu (Masalmo 24:1; 1 Akorinto. 4:7). Muyenera kuzindikira kuti ndinu wongoyang'anira chuma cha Mulungu, ndipo tsiku lina mudzayankha mlandu kwa Iye za momwe munasamalirira chuma chanu (Luka 16:2).

Dongosolo labwino la kasamalidwe ka ndalama ndikugawa ndalama zanu m'magulu atatu akuluakulu: Choyamba, mumapereka kwa Mulungu; ndiye, mumasungira mtsogolo; ndipo potsiriza, mumagwiritsa ntchito mwanzeru pa zosowa zapano. Tiyeni tione bwinobwino dongosolo la magawo atatu ili la kasamalidwe ka ndalama mwaumulungu.

1. Choyamba, mumapereka kwa Mulungu. Monga Mbusa wachipentekoste, kupereka mowolowa manja ndi gawo lanu loyamba kuti mukhale ndi moyo wabwino pazachuma. Lemba limatiuza mobwerezabwereza kuti zipatso zoyamba za chirichonse chimene timalandira ndi cha Mulungu (Eksodo 13:1; 34:26; Levitiko. 2:14; Miyambo 3:9). Chifukwa chake, chinthu choyamba pakuwongolera chuma chanu ndikupereka mokhulupirika chakhumi chanu ndi zopereka kwa Mulungu. Muyenera kukwaniritsanso malonjezano ena aliwonse azachuma omwe mwapanga kwa Iye kapena mpingo Wake, monga utumwi ndi malonjezano a thumba la zomangamanga. Mulungu akulonjeza kudalitsa mochulukira iwo amene ali owolowa manja ndi Iye (Malaki 3:10-11; Luka 6:38).

2. Kenako, mumasungira zam'tsogolo. Mukapereka kwa Mulungu, muyenera kusungira zosowa zamtsogolo komanso zadzidzidzi. Mungachite zimenezi poika ndalama zoikidwa mu akaunti yosunga ndalama sabata lililonse. Pamene akauntiyi ikukula, ikhoza kukhala ngati njira yotetezera ngozi, ndipo ikhoza kukhala gwero la ndalama zogulira zinthu zazikulu.

3. Pomaliza, gwiritsani ntchito mwanzeru. Zomwe zimatsalira pambuyo popereka kwa Mulungu ndi kusunga ndalama zingagwiritsiridwe ntchito kukwaniritsa zofunika za banja, monga chakudya, nyumba, ndi zina. Pakuti ndalama zimenezinso ndi za Mulungu, muzizigwiritsa ntchito mwanzeru. Njira

yabwino yochitira izi ndi kupanga ndondomeko (bajeti) yotheka, kapena dongosolo lazachuma. Dongosololi likhala ngati chiwongolero pakugwiritsa ntchito ndalama, ndipo lidzakuthandizani kugula zokhazo zomwe mumafuna. Ndalama zosamalidwa bwino zidzakuthandizani kubweretsa mtendere ndi bata m'nyumba mwanu. Ndipo zidzakuthandizani inuyo ndi banja lanu kukwaniritsa zolinga zanu.

Kusamalira Nthawi

Chachiwiri, kuti mukhale ndi moyo woyendetsedwa bwino, muyenera kuphunzira kugwiritsa ntchito bwino nthawi yanu. Chifukwa cha zochitika za chikhalidwe zina, abusa ambiri a mu Afirika amawona kugwiritsira ntchito nthaŵi kukhala kovuta. Komabe, nthawi ndi chinthu chamtengo wapatali kwambiri cha munthu. Ngakhale kuti titha kupezanso ndalama zomwe zatayika, sitingabwezeretse nthawi yomwe idatayika. Baibulo limatilimbikitsa kuombola nthaŵi mwa kugwiritsira ntchito bwino mpata uliwonse (Aefeso 5:15-16; Akolose. 4:5).

Monga Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste, monganso muyenera kuphunzira kuwerengera ndalama zanu, muyenera kuphunzira kukonza nthawi yanu. Muyenera kuphunzira kugawa nthawi yochitira banja, ntchito, yopuma, yophunzira, yopemphera, yochezera, ndi zinthu zina zofunika. Ntchitoyi idzafuna kuti mupange mndandanda wa zochita, kukonza malo ogwirira ntchito, kupanga zochitika za tsiku ndi tsiku ndi sabata, ndikupewa kuzengereza.

Kudzisamalira

Chachitatu, pofunafuna moyo woyendetsedwa bwino, muyenera kuphunzira kudzisamalira nokha. Kudzisamalira ndiko kuchita zofuna zathu zauzimu, zamaganizo, ndi zakuthupi. Timachita zimenezi, osati chifukwa cha dyera, koma pazifukwa zaumulungu. Timadzisamalira tokha kuti titumikire bwino Mulungu ndi anthu ena.

Pamene Mulungu analenga anthu, anawalenga ndi mzimu, moyo, ndi thupi (1 Atesalonika. 5:23). Mzimu ndi gawo la mwamuna kapena mkazi limene limalankhula ndi Mulungu. Moyo ndi gawo limene limaganiza, kumva, ndi kusankha. Ndipo thupi ndi mbali ya thupi la munthu. Thupi ndi nyumba yomwe mzimu ndi moyo wathu zimakhalamo. Kudzisamalira kumaphatikizapo kusamalira magawo onse atatu.

Mutha kusamalira mzimu wanu ndi moyo wanu podzipatsa mwambo wa uzimu monga kusinkhasinkha pa Mawu, kupembedza, kupemphera, ndi kusala kudya[2]. Kuonjezera apo, muyenera kudzipereka mosalekeza maganizo anu, maimvaimva anu, ndi chifuniro chanu ku ufumu wa Khristu. Baibulo limatilangiza kuti: "Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuniro cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro" (Aroma 12:2). Baibulolimatiphunzitsanso mmene tiyenera kuyendera maganizo athu:

"Zinthu zilizonse zoona, zilizonse zolemekezeka, zilizonse zolungama, zilizonse zoyera, zilizonse zokongola, zilizonse zimveka zokoma; ngati kuli chokoma mtima, kapena chitamando china, zilingirireni izi" (Afilipi. 4:8).

Kusamalira matupi athu ndikofunikira chifukwa matupi athu ndi akachisi a Mzimu Woyera. Choncho tiyenera kulemekeza Mulungu ndi matupi athu (1 Akorinto 6:19-20). Thupi lathanzi limatithandiza kukwaniritsa bwino maitanidwe a Mulungu pa miyoyo yathu. Zimatithandiza kukhala ndi moyo wokwanira (Yohane 10:10). Chotero tiyenera kusamalira matupi athu mwa kudya bwino, kuchita masewera olimbitsa thupi nthawi zonse, kugona mokwanira, ndi kupita kuchipatala nthawi zonse.

KUTSATIRA MOYO WOSAMALIDWA BWINO

Mwina mungafunse kuti, "Kodi ineyo monga Mbusa wa Chipentekoste ndingatani kuti ndikhale ndi moyo wabwino?

Kapanga Chiganizo

Mumayamba kufunafuna moyo woyendetsedwa bwino ndi chisankho. Yesu anafotokoza nkhani ya Mwana Wolowerera. M'nkhaniyi, mwana wopandukayo anafuna cholowa kwa bambo ake n'kuchoka panyumba. Posakhalitsa, chifukwa cha moyo wake wodzikonda, mnyamatayo anapezeka ali kutchire kudyetsa nkhumba. Pa nthawiyo, mwanayo anabwerera m'maganizo, n'kunena kuti: "Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, Atate, ndinachimwira Kumwamba ndi pamaso panu, sindiyeneranso konse kutchulidwa

[2] Mutu uwu wakambidwa pa Mutu 15: "Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu."

mwana wanu; mundiyese ine ngati mmodzi wa antchito anu" (Luka 15:18-19). Ndi chiganizo chimenecho, ananyamuka n'kuyamba ulendo wobwerera kwawo.

N'chimodzimodzinso ndi kufunafuna moyo woyendetsedwa bwino. Ulendo wanu wopita ku moyo wopindulitsa uyenera kuyamba ndi chisankho cholimba. Muyenera kuyang'ana momwe mulili pano ndikuwona kuti pali njira yabwino yokhalira ndi kutumikira. Muyenera kunena kuti, "Ndinyamuka ndikulondola moyo (machitachita) wopindulitsa kwambiri."

Pangani Dongosolo

Ngakhale kuti kusankha kukhala ndi moyo woyendetsedwa bwino n'kofunika kwambiri, sizokhazi ayi. Chosankha chanu chiyenera kutsatiridwa ndi ndondomeko yotheka. Dongosololi liphatikiza njira zitatu, motere:

1. Kudziyesa. Mumayamba ulendo wanu wopita ku moyo wosamalidwa bwino ndi kudziyesa nokha. Mukudzifufuza uku, mukuona moyo wanu wapano kuti muzindikire pomwe ukufunika kusintha. Mungachite zimenezi mwa kuyankha moona mtima mafunso ngati awa:

- Kodi ndikuchita bwino bwanji posamalira chuma changa?
- Kodi ndikuchita bwino motani pakugwiritsa ntchito nthawi yanga?
- Kodi ndikuchita bwino motani posamalira mzimu, moyo, ndi thupi langa?
- Kodi ndingachite bwino bwanji m'mbali zonsezi?

Yankhani mafunsowa mosamala, ndipo lembani mayankho anu m'kope.

2. Kukhazikitsa zolinga. Mukazindikira madera omwe mukufunikira kusintha, khalani ndi zolinga zanu zachitukuko. Mungachite zimenezi mwa kufunsa ndi kuyankha moganizira mafunso otsatirawa

- Ndi njira ziti zomwe ndikufuna kupititsa patsogolo luso langa la kasamalidwe ka chuma?
- Kodi ndikufuna kukulitsa luso langa logwiritsa ntchito nthawi yanji?
- Kodi ndikufuna kukulitsa luso langa losamalira mzimu, moyo, ndi thupi langa?

Apanso, lembani mayankho anu m'kope lanu. Nenani molunjika.

3. Kupanga dongosolo. Mukakhazikitsa zolinga zanu, muyenera kupanga dongosolo kuti mukwaniritse zolingazi. Ganizirani za nkhani imodzi kapena ziwiri zokha panthawi imodzi, ndipo pangani ndondomeko yoti mukwaniritse cholinga chilichonse. Mu dongosolo lanu, mudzafuna kudziwa njira zomwe mungatenge kuti mukwaniritse zolinga zanu. Mwachitsanzo, mungafune kukulitsa luso lanu lazachuma mwa kupanga ndi kutsatira bajeti yabanja. Kapena, mungafune kukulitsa luso lanu la kasamalidwe ka nthawi polemba zochita m'mawa uliwonse, kenako ndikugwiritsa ntchito mndandandawu kuwongolera zomwe mumachita tsiku lililonse.

Kagwireni Ntchito

Mukapanga dongosolo lanu, muyenera kuchitapo kanthu. Muyenera kuyamba kupanga dongosolo lanu. Khalani wolimbikira; khalani ndi dongosolo lanu. Kenako, pakutha kwa miyezi itatu kapena isanu ndi umodzi, fufuzani ngai mukupita chitsogolo. Dziwani pamene mwachita bwino ndi pomwe simunachite bwino. Kenako, sinthani dongosolo ndikubwereza ndondomekoyi. Mungafune kupitirizabe kuchita zinthu zomwezo, kapena mungafune kukwaniritsa zolinga zina.

Kupeza moyo woyendetsedwa bwino ndi ntchito ya muyaya. Ndi cholinga choyenera kutsata, ndipo chidzabweretsa madalitso ambiri mu moyo wa Mbusa wa Chipentekoste.

~ Mutu 14 ~

Maubale Abwino

Katswiri wina wa Chilamulo cha Mose anapita kwa Yesu ndi funso. "Mphunzitsi," anafunsa motero, "lamulo lalikulu ndi liti la m'chilamulo? Mosazengereza, Yesu anamuyankha kuti: "Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndili, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini" (Mat. 22:36-39). Chotero, malinga ndi kunena kwa Yesu, maubale ndiwo maziko a tanthauzo la kutumikira Mulungu.

Chikhristu ndi choposa chipembedzo; ndi ubale waumwini ndi Mulungu kupyolera mwa Yesu Khristu. Si nkhani yongotsatira zikhulupiriro zinazake kapena kuchita miyambo inayake. M'malo mwake, ndi nkhani ya kukonda Mulungu ndi ena. Lingaliro limeneli la ubale wachikondi ndi Mulungu ndi anthu limasiyanitsa ChiKhristu ndi zipembedzo zina.

Utumiki wa ubusa uyenera kuchitidwa pafupi ndi mpingo. Monga mmene Mbusa sangasamalire nkhosa zake ali patali, Mbusa wa Pentekoste sangasamalire anthu akutali. Kuti akhale opambana mu utumiki, Mbusa wa Pentekoste ayenera kumvetsetsa kufunikira komanga maubale olimba, athanzi. Ndipo ayenera kudziwa momwe maubwenzi amenewa amakulira ndi kusungidwira.

KUMVETSETSA MAUBWENZI

Ubale ndi mgwirizano womwe timapanga wina ndi mnzake. Ndi njira zomwe timalumikizana wina ndi mzake. Maubwenzi amatha kukhala apafupi kapena akutali, amphamvu kapena ofoka, enieni kapena ongoyerekeza, athanzi kapena owononga. Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kudziwa momwe mungamangire ubale wabwino ndi achibale, mamembala ampingo, abwenzi, ndi abusa ena. Ndipo inunso muyenera kuphunzitsa ena kuchita chimodzimodzi.

Maubwenzi abwino amalola anthu a Mulungu kukhalira limodzi mogwirizana. Amadalitsa anthu ndi kuwalimbikitsa. Amawathandiza kudzimva kukhala otetezeka, olemekezedwa, ndi olandiridwa. Ubale wabwino umagwirizanitsanso anthu a Mulungu m'ntchito zopindulitsa. Iwo amapangitsa kuti mpingo ukhale wopambana ndi kukhala wolimba. Kumbali ina, maubwenzi osayenera amapangitsa anthu kugwa m'mikangano ndi mkwiyo. Ubale woterewu umapangitsa kuti mpingo ukhale wofooka komanso wosagwira ntchito.

Chotero Paulo analimbikitsa Akhristu oyambirira kukulitsa maunansi abwino kwa wina ndi mnzake. Iye analembera Akhristu a ku Aefeso kuti chitani chilichonse chotheka "ndi kusamalitsa kusunga umodzi wa Mzimu mwa chimangiriro cha mtendere." (Aefeso 4:3). Iye analangizanso okhulupirira a ku Roma kuti: "Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzake. Musasamalire zinthu zazikulu, koma phatikanani nao odzichepetsa. Musadziyesere anzeru mwa inu nokha" (Aroma 12:16). N'chimodzimodzinso ndi anthu odzikuza. Paulo anazindikira kuti maunansi abwino ndi maziko a utumiki wogwira mtima mkati ndi kunja kwa mpingo.

MITUNDU YA MAUBWENZI

Monga Mbusa wa Chipentekoste, ndikofunikira kuti mudziwe zamitundu yosiyanasiyana ya maubale omwe mumakumana nawo m'moyo. Kumvetsetsa uku kudzakuthandizani kuyika patsogolo maubwenzi omwe muyenera kuwasamalira kwambiri.

Ubwenzi Woyamba

Ubwenzi wanu wofunika kwambiri m'moyo ndi ubwenzi wanu ndi Mulungu. Maubwenzi ena onse ayenera kumangidwa pa ubale woyambawu. Choncho muyenera kuika ubwenzi wanu ndi Mulungu patsogolo. Ngati mumvetsetsa bwino

ubalewu, maubwenzi ena onse amakhazikika. Ndipo ngati mutasokoneza ubalewu, maubwenzi ena onse adzakhudzidwa.

Ubale wanu ndi Mulungu uyenera kukhala wa chikondi chakuya (Mateyu 22:37). Kukonda Mulungu kumeneku kudzaonekera mwa kumvera modzipereka ku malamulo Ake (Yohane 14:15, 21) ndiponso poganizira ena mwachikondi (Yohane 15:12).

Ubwenzi wa pa Banja

Chachiwiri pa ubale wanu ndi Mulungu ndi ubale wanu ndi mwamuna kapena mkazi wanu. Baibulo limanena kuti Mulungu analenga mwamuna ndi mkazi kukhala thupi limodzi (Genesis. 2:24). Chifukwa chake mwamuna azikonda mkazi wake monga akonda thupi la iye yekha, monganso Khristu akonda Eklesia. Ndipo mkazi ayenera kulemekeza mwamuna wake ndi kugonjera ulamuliro wake m'banja (Aefeso 5:21-33). Choncho, inu ndi mwamuna kapena mkazi wanu muyenera kuyamikira ubwenzi umenewu kuposa maubale ena onse aanthu. Ndipo muyenera kuyika nthawi yokwanira komanso kuyesetsa kulimbitsa ubalewu.

Ubale wanu wachitatu wofunika kwambiri ndi ana anu. Muyenera kukonda kwambiri ana anu, ndi kuwasamalira mwachikondi. Baibulo limanena kuti makolo ayenera kulera ana awo m'malangizo a Yehova (Aefeso 6:4). Choncho, musanyalanyaze ana anu-ngakhale mukuchita ntchito zaubusa. M'malo mwake, muyenera kupeza nthaŵi yopanga ubwenzi ndi aliyense wa iwo. Zimenezi zidzachititsa kuti m'banja mukhale ubwenzi wachikondi. Mkhalidwe umenewu udzakulolani kuti mugwire ntchito yanu mwamtendere, ndipo mudzakulitsa zokolola zanu muutumiki. Zidzakhalanso umboni kwa mpingo ndi anthu am'mudzi. Chofunika koposa, muyenera kuyesetsa kutsogolera ana anu kukhala paubale ndi Khristu. Ndipo muonetsetse kuti mwana aliyense wadzazidwa ndi Mzimu Woyera.

Komanso, muyenera kukulitsa ubale wachikondi ndi achibale anu. Muyenera kusonyeza chikondi choyenera cha Chikhristu ndi ulemu kwa makolo anu, abale ndi alongo anu, asuweni anu, ndi ziwalo zina zabanja. Muyenera kusunga zinthu zonse mu dongosolo lawo loyenera. Musamakonde achibale anu kuposa mwamuna kapena mkazi wanu ndi ana anu. Paulo analembera Timoteo kuti: "Koma ngati wina sadzisungiratu mbumba yake ya iye yekha, makamaka iwo a m'banja lake, wakana chikhulupiriro iye, ndipo aipa koposa wosakhulupirira" (1 Tim. 5:8)[1]

Ubale wa Utumiki

Kuphatikiza pa ubale wanu ndi Mulungu ndi achibale anu, ngati mbusa wa Chipentekoste, muyenera kusamala ubale wanu wa utumiki. Maubale amenewa akuphatikizapo onse amene mumawatumikira komanso amene mumatumikira nawo. Amaphatikizapo mamembala ampingo wanu, dera lanu, ndi chipembedzo chanu kapena tchalitchi cha dziko. Ubale uliwonse ndi wapadera, ndipo uliwonse uyenera kuchitidwa mosiyana pang'ono. Pamlingo waukulu, kupambana kwanu kapena kulephera kwanu muutumiki kudzadalira momwe mumayendetsera maubwenzi awa.

Kupitilira apo mufunika kukhala ndi ubale wamphamvu komanso waukadaulo ndi abusa ndi anthu wamba ampingo wanu. Yesu atasankha atumwi 12 aja, anawatuma kuti akalalikire ndi kutulutsa ziwanda. Komabe, poyamba anawaitana kuti akacheze naye (Marko 3:13-15). Ambuye wathu anadziwa kuti chomangira chimene iye adzamanga nawo pamene iwo ali pamodzi chidzakhala maziko a utumiki wawo pamene iwo anali kutalikirana. N'chimodzimodzinso ndi mpingo umene mumatsogolera. Ubale wanu ndi abusa ndi antchito anu udzakhala maziko a utumiki wonse mu mpingo.[1]

Maubwenzi Atatu Oopsa

Maubwenzi ena amabwera ndi mulingo wowopsa. Zitatu mwa maubwenzi amenewo ndi ubwenzi wanu ndi dziko, ubwenzi wanu ndi anthu amene si amuna kapena akazi anzanu, ndiponso mabwenzi amene mumasankha. Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuyang'ana maubale awa mosamala kwambiri, motere:

1. Ubale wanu ndi dziko lapansi. Muyenera kukhala tcheru mu ubale wanu ndi dziko. Dziko lapansi lapangidwa ndi machitidwe ambiri a padziko lapansi olamulidwa ndi Satana ndi iwo amene amamtumikira (1 Yohane 5:19). Yesu anauza ophunzira ake kuti: "Simuli a dziko lapansi, koma Ine ndinakusankhani inu mwa dziko lapansi" (Yohane 15:19). Baibulo limafotokoza kuti, ngakhale kuti wotsatira Khristu ayenera kukhala m'dzikoli, sayenera kutengeka ndi zinthu za m'dzikoli (1 Ako. 7:31). Asamakonde zinthu za dziko (1 Yohane 2:15). Komanso sayenera kutengera makhalidwe a dziko lapansi (Aroma 12:2).

2. Ubwenzi wanu ndi munthu amene siali wa mwamuna kapena mkazi nzanu. Ndiponso, monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kusamala kwambiri ubale wanu ndi anthu amene si amuna kapena akazi anzanu. Chifukwa chakuti abusa ena alephera kusunga malire muubwenzi umenewu, agwa m'manyazi ndipo

achititsa manyazi ntchito ya Mulungu. Paulo anachenjeza Timoteo kuti: "Thawa zilakolako za unyamata, nutsate chilungamo" (2 Tim. 2:22). Iye analangizanso mwana wake m'chikhulupiriro kuti: "[Chitira] akazi aakulu ngati amai, ndi akazi aang'ono ngati alongo, m'kuyera mtima konse" (1 Tim. 5:2).

Muyenera kugwirizana kwambiri ndi amuna kapena akazi anzanu moyenerera. Kupatulapo mwamuna kapena mkazi wanu, musamapezeke nokha ndi munthu yemwe si mwamuna kapena mkazi mnzanu. Muyeneranso kuteteza maganizo anu. Chigololo chilichonse chimayamba m'malingaliro amunthu. Choncho, musalole maganizo anu kuchoka kwa mwamuna kapena mkazi wanu kupita kwa munthu wina (Mateyu 5:28). Baibulo limatilangiza kuti: "Koposa zonse uzisunga; pakuti magwero a moyo atulukamo" (Miyambo. 4:23)

3. Anzanu amene mumasankha. Kusankha abwenzi kungabweretse madalitso akulu kapena chivulazo chachikulu m'moyo wa Mbusa. Choncho muyenera kugwiritsa ntchito nzeru posankha abwenzi. Baibulo limatiuza kuti: "Wolungama atsogolera mnzake; koma njira ya oipa iwasokeretsa" (Miy. 12:26). Anthu oipa amasocheretsa. Paulo anawonjezera kuti: "Musanyengedwe; mayanjano oipa aipsa makhalidwe okoma (1 Ako. 15:33). Monga Mbusa wa Pentekoste, muyenera kupanga maubwenzi olimba ndi anthu okhawo amene angakulimbikitseni kuyandikira kwa Mulungu ndi kukhala ndi moyo wokondweretsa Mulungu.

MAKHALIDWE A UBWENZI WABWINO

Anthu a ku Afirika amazindikira kuti khalidwe la moyo wa munthu limatsimikiziridwa makamaka ndi ubwino wa maubwenzi ake. Nanga ndi zizindikiro ziti zomwe Mbusa wa Chipentekoste angagwiritse ntchito powatsogolera pomanga ndi kusunga ubale wabwino m'nyumba zawo, mipingo ndi madera awo? Monga Mbusa wa Chipentekoste, maubale anu ayenera kuonetsa makhalidwe asanu:

Chikondi

Khalidwe loyamba lomwe liyenera kufotokozera ubale wanu ndi ena ndi chikondi chopereka nsembe. Muyenera kukonda mwamuna kapena mkazi wanu, ana anu, ndi anthu a Mulungu ndi chilakolako chomwecho chimene Khristu amakukondani inu. Yesu analamula ophunzira ake kuti: "Monga ndakonda inu, inunso mukondane wina ndi mnzake" (Yohane 13:34). Anali kuwauza kuti chikondi chopanda dyera chiyenera kusonyeza ubale wawo ndi wina ndi mnzake.

Yesu anali wokonzeka kupereka moyo wake chifukwa cha iwo. Tsopano, ayenera kukhala okonzeka kupereka moyo wawo chifukwa cha wina ndi mnzake (Yohane 15:12-13). N'chifukwa chake Petro akutilimbikitsa kuti: "Mukondane kwenikweni kuchokera kumtima" (1 Petro. 1:22) Choncho tiyenera kukondana kwambiri.

Kulankhulana Mowona mtima

Khalidwe lachiŵiri limene liyenera kusonyeza ubale wanu ndi ena ndilo la kulankhulana momasuka, komanso mowona mtima. Paulo analangiza Akhristu a ku Aefeso kuti azilankhula zoona mwachikondi. Akadachita izi, akadakula ndi kukhwima ngati thupi lake (Aef. 4:15). Mtumwiyu anapitiriza kulangiza Akhristu a ku Akolose kuti: "Mau anu akhale m'chisomo, okoleretsa, kuti mukadziwe inu mayankhidwe anu a kwa yense atani" (Akolose. 4:6).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kulingalira mosamalitsa mawu anu musanalankhule, mukukumbukira mawu a m'Malembo akuti: "Wogwira pakamwa pake asunga moyo wake; koma woyasamula milomo yake adzaonongeka" (Miy. 13:3).Kulankhulana kwanu ndi ena kuyenera kukhala kwaubwenzi, chidaliro, ndi kuona mtima. Mawu anu ayenera kukhala wobweretsa mtendere, osalankhula mwaukali koma moona mtima ndi chifundo. Ndipo muyenera kuphunzira kumvetsera mwatcheru zimene ena akunena. Baibulo limatilangiza kuti: "Wobwezera mau asanamvetse apusa, nadzichititsa manyazi" (Miy. 18:13).

Kukhulupirirana wina ndi Nzake

Khalidwe lachitatu lomwe liyenera kufotokozera ubale wanu ndi banja lanu komanso mamembala ampingo ndikukhulupirirana. Chikhulupiriro ndi chidaliro chimene anthu amakhala nacho mwa wina ndi mnzake. Kukhulupirirana ndi chidaliro chogawana chakuti onse omwe ali pa ubwenzi adzakhala oona komanso kuti adzakhala odzipereka ku chiyanjano. Kuti kukhulupirirana kuchitike, onse amene ali muubwenzi ayenera kusonyeza kudzipereka kwawo kwa wina ndi mnzake.

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutsimikizira kuti anthu ayenera kukudalirani. Anthu ayenera kumva kuti ali otetezeka kuti ali ndi abusa awo. Ayenera kumva kukhala omasuka ponena zinsinsi zawo zozama. Ndipo ayenera kudziwa kuti abusa awo sauza ena zinsinsi zimenezi.

Ulemu

Khalidwe lachinayi limene liyenera kusonyeza ubwenzi wanu ndi ena ndilo kulemekezana. Ulemu ndi kulemekeza kwambirimaganizo, ufulu, ndi kulemekeza ena. Petro analimbikitsa Akhristu kuti: "Chitirani ulemu anthu onse" (1 Petro. 2:17) Akazi azilemekeza amuna awo ndipo amuna azilemekeza akazi awo. Ana ayenera kulemekeza makolo awo, ndipo makolo ayenera kulemekeza ana awo. Mamembala a mpingo ayenera kulemekeza abusa awo, ndipo abusa awo ayenera kulemekeza ma membala.

Chifukwa chakuti anthu onse ali ndi chifaniziro cha Mlengi wawo, muyenera kulemekeza munthu aliyense mosasamala kanthu monga fuko, mtundu, kapena zochita zawo. Paulo analimbikitsa Akhristu a ku Roma kuti "azikhala odzipereka kwa wina ndi mnzake" komanso "mutsogolerane ndi kuchitira wina mnzake ulemu" (Aroma 12:10). Iye anawonjezera kuti: "Mukhale ndi mtima umodzi wina ndi mnzake. Musasamalire zinthu zazikulu, koma phatikanani naoodzichepetsa. Musadziyesere anzeru mwa inu nokha" (v. 16).

Kudzichepetsa

Pomaliza, ubwenzi wanu ndi ena uyenera kukhala wodzichepetsa. Kudzichepetsa n'kosiyana ndi kudzikuza. Kudzikuza ndiko kumasuka ku kunyada. Kudzichepetsa ndiko kuthekera kwa munthu kudziona monga momwe Mulungu amamuonera. M'mawu ena, munthu wodzichepetsa amatha kudziona ngati mmene alili. Kudzichepetsa kumasonyeza chikondi chenicheni. Paulo analemba kuti: "Chikondi…sichidziwa kudzitamanda, sichidzikuza; sichichita zosayenera, sichitsata za mwini yekha, sichipsa mtima, sichilingirira zoipa" (1 Akorinto 13:4-5).

Kunyada kumatseka chitseko cha maubale ozama komanso okhalitsa. Kudzichepetsa kumatsegula chitseko chimenechi (Aroma 12:16). Monga Mbusa wodzichepetsa, mudzakhala mwamuna kapena mkazi wa anthu. Mudzakhala ofikirika. M'malo momanga makoma pakati pa inu ndi anthu, mudzamanga milatho.

KUSUNGA NDI KUSAMALIRA UBWENZI WABWINO

Nazi zinthu zitatu zimene zingakuthandizeni kumanga ndi kusunga ubale wabwino ndi wolemekeza Mulungu ndi ena:

Kukhala ndi cholinga

Choyamba, muyenera kukhala ndi cholinga chomanga ndi kusunga maubwenzi abwino ndi achibale anu, mamembala ampingo, ndi abwenzi anu otumikira. Muyenera kuchitapo kanthu ndikutsata maubalewa mwachangu. Izi n'zimene Yesu anachita. Iye anasankha kuyenda pakati pa anthu. Anapeza nthawi yowamvetsera komanso kumva kulira kwawo. Adani ake anaona zimenezi, ndipo anamuimba mlandu wa "bwenzi la amisonkho ndi ochimwa" (Mateyu 11:19). Adani akewo anazindikira zimenezi. Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuyesetsa kukhala ngati Yesu ndikuyesetsa mwakhama kumanga ubale wolimba ndi ena.

Samalirani ma Ubwenzi

Komanso, muyenera kuyesetsa kuti mukhale ndi ubale wabwino. Muyenera kukhala okonzeka kugwiritsa ntchito nthawi ndi mphamvu zomwe zikufunika kuti mumange maubwenzi olimba, okhalitsa ndi banja lanu, mamembala ampingo wanu, ndi abwenzi anu otumikira. Kuti muchite izi, muyenera kukhala nawo nthawi, kumvetsera nkhani zawo, kuseka nthabwala zawo, ndi kulira chifukwa cha zowawa ndi zolephera zawo (Aroma 12:15). Ngati muchita zimenezi, m'kupita kwa nthaŵi, chikondi champhamvu chidzapanga pakati pa inu ndi anthu anu.

Khalani Okhululuka

Pomaliza, ngati mukufuna kumanga ndi kusunga maubwenzi olimba, okhalitsa ndi ena, muyenera kuphunzira kupempha ndikupereka chikhululukiro. Ndizosapeweka; anthu adzakhumudwa, ndipo adzakhumudwa. Kusamvana kudzachitika ndipo tidzamva kuwawa mmoyo wathu. Kuti maubwenzi asungidwe, kukhululuka kuyenera kuchitika.

Nkhope ya chikhululukiro ili ndi mbali ziwiri. Mbali imodzi ndi wolakwayo wopempha chikhululukiro. Mbali ina ndi munthu wolakwiridwayo kupereka chikhululukiro. Muyenera kukhala okonzeka kuchita zonse ziwiri (Mateyu 5:22-26). Muyenera kufulumira kupempha chikhululukiro pamene mwalakwiridwa. Ndipo muyenera kukhala okonzeka kukhululukira munthu wina akakupemphani.

Kukhululuka kumamasula wolakwira ndi wolakwiridwayo. Kumatsegula makomo a chiyanjanitso ndi kupanga njira yoti maubwenzi osweka akonzedwenso.

Utumiki wabwino umamangidwa pa maubwenzi olimba, abwino. Mbusa wanzeru wa Chipentekoste adzaika luntha lochuluka pomanga maubale amenewa.

~ Mutu 15 ~

Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu

Komatu zenizeninso ndiyesa zonse zikhale chitayiko chifukwa cha mapambanidwe a chizindikiritso cha Khristu Yesu Ambuye wanga" (Afilipi 3:8). Awa ndi mawu a mtumwi Paulo. Kupatulako Yesu, zimakhulupirika kuti iye ndi mtumwi woposa onse amene anakhalako. Analalikira ndi mphamvu, anachita zozizwitsa, ndipo anadzala mipingo mu Ufumu wonse wa Roma. Mulungu anamugwiritsa ntchito kutsegula khomo la chipulumutso kwa amitundu (Machitidwe 14:27). Komabe, m'zonsezi, iye anawona kuti chimene Iye anachita chachikulu m'moyo chinali kungodziwa Yesu. Pemphero lake lokhazikika linali lakuti, "kuti ndimzindikire Iye" (Afilipi 3:10).

Monga Paulo, inu ngati Mbusa wa Chipentekoste ndinumtsogoleri. Motero, muli ndi maudindo ambiri. Mwaitanidwa kukulitsa okhulupirira kukhala ophunzira ndi kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu padziko lapansi. Izi ndi ntchito zazikulu, ndipo muyenera kuchita izi mokhulupirika. Komabe, ngati mukufuna kupita kutali muutumiki, monga Paulo, muyenera kuika patsogolo ubale wanu ndi Khristu. Muyenera kudzipereka nokha kudziwa Khristu ndi kuphunzira kukhala mu chiyanjano chosalekeza ndi Iye.

Kuti muchite izi, muyenera kukhala ndi chizolowezi champhamvu chachipembedzo. Ngakhale ntchito yochuluka bwanji, kaya ikhale yofunika

kapena yogwira mtima chotani, isadzapangitse chiyanjano ndi Ambuye kusokonekera. Mutu uwu ufotokoza za chizolowezi chodzipereka cha Mbusa wa Chipentekoste.

CHIZOLOWEZI CHODZIPEREKA

Tiyamba kufufuza kwathu za chizolowezi chodzipereka ndi matanthauzo a mau ena.

Kumvetsetsa Tanthauzo

Chizolowezi ndi zimene munthu amachita nthawi zonse. Ndi khalidwe lobwerezabwereza lomwe lakhazikika pamoyo. Mofanana ndi munthu amene akutsuka mano m'mawa uliwonse, zizolowezi zimakula mwa kubwerezabwereza. Pachiyambi, munthu ayenera kudzikumbutsa yekha kufunika kochita ntchitoyo. Ndipo nthawi zina amafunikira kudzilanga kuti achite zimenezo. Komabe, pakapita nthawi, ntchitoyo imakhala chizolowezi.

Nanga chizolowezi chodzipereka ndi chiyani? Chizolowezi cha kupembedzera ndi mwambo wachikhristu wosunga nthawi ya chiyanjano ndi Khristu tsiku ndi tsiku. Ndi nthawi imene mtumiki wokhulupirika wa Khristu amapatula tsiku lililonse kuti akulitse ubale wake ndi Mulungu. Ndi chizolowezi chifukwa, m'kupita kwa nthawi, chimakhala chochitidwa nthawi ndi nthawi. Ndi kudzipereka chifukwa cholinga chake ndi kukulitsa ubale wa munthu ndi Mulungu ndikuwonjezera kudzipereka kwawo kwa Iye ndi ntchito yake.

Ubwino wa Chizolowezi Chopembedzera

Ngati mukulitsa ndi kukhalabe wokhulupirika ndi chizolowezi chodzipereka champhamvu, mapindu ambiri adzabwera m'moyo wanu ndi utumiki wanu. Tiyeni tiwone zinai mwa zabwinozo:

1. *Kudziwa Khristu*. Phindu loyamba la kukhala ndi chizolowezi chodzipereka champhamvu ndi chakuti chidzakupangitsani kukula mu ubale wanu ndi Khristu. Wolemba buku la Ahebri amatilimbikitsa kuti: "Tiyandikire ndi mtima woona" (Ahebri. 10:22) Choncho tiyenera kuyandikira kwa Mulungu. Yakobo anawonjezera lonjezo ku lamulo lakuti: "Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu" (Yakobo 4:8). Pamene mukupemphera ndi kusinkha-sinkha Mau a Mulungu, mudzalowa mu malo opatulikitsa (Ahebri. 10:19). Kumeneko, pamaso pa Mulungu, inu, monga Mose wakale, mudzapezeka

mukulankhulana ndi Mulungu “maso ndi maso, monga munthu alankhula ndi bwenzi” (Eksodo. 33:11).

2. Kuzindikira chifuniro cha Mulungu. Phindu lachiwiri la kukulitsa chizolowezi chanu chodzipereka champhamvu ndi chakuti mudzafika pakumvetsetsa bwino chifuniro cha Mulungu pa moyo wanu. Pamene mupemphera, kuwerenga Mawu a Mulungu, ndi kugwiritsira ntchito ziphunzitso zake m’moyo wanu, maganizo anu adzasandulika. Izi zikachitika, “kuti mukazindikire chimene chili chifuniro cha Mulungu, chabwino, chokondweretsa ndi changwiro” (Aroma 12:2).

3. Kukulitsa kawonedwe ka Baibulo. Phindu lachitatu la kukulitsa chizolowezi chodzipereka champhamvu ndi chakuti mchitidwewo udzakuthandizani kukulitsa kuzindikira kwanu kwa malemba. Pamene mukufufuza Malemba mwapemphero, mudzayamba kuona Baibulo momwe Mulungu amalionera. Mudzayamba kumvetsetsa dongosolo Lake la anthu. Ndipo mudzatha kuzindikira malo anu pokwaniritsa dongosolo limenelo.

4. *Kukhala mu chiyanjano ndi Mzimu*. Phindu lachinayi lakukhalabe ndi chizolowezi chodzipereka champhamvu ndi chakuti mudzaphunzira kukhala mu chiyanjano ndi Mzimu Woyera (2 Ako. 13:14). Paulo analimbikitsa Akhristu kuti “ndi Mzimunso tiyende” (Agal. 5:25). Anawalangizanso kuti, “Mudzale naye Mzimu” (Aef. 5:18). Mu chikhalidwe cha kudzipereka, Mzimu Woyera adzadziwitsa mphamvu zake ndi kupezeka kwake. Zili ngati magetsi kuchokera kugwero lamagetsi kupita ku babu. Malingana ngati chingwecho chalumikizidwa ku magetsi, babu limayaka. Komabe, chingwecho chikachotsedwa, mphamvuyo imasiya kuyenda ndipo babu limazima. Kupyolera mu chizolowezi chodzipereka, mutha kukhala olumikizidwa ku gwero lamphamvu. Mutha kukhalabe odzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu.

ZOFUNIKIRA NDI MACHITACHITA A CHIZOLOWEZI CHODZIPEREKA

Mafunso awiri akubuka: “Kodi inu, monga Mbusa wa Chipentekoste, mungatani kuti mukhale ndi chizolowezi champhamvu chodzipereka?” ndi "Kodi muyenera kuchita chiyani kuti mupindule kwambiri ndi ntchitoyi?"

Nkhani Zitatu Zofunika

Kuti mukhale ndi chizolowezi chodzipereka kwambiri, muyenera kuwonapo zinthu zitatuzi:

1. *Zofunika Kwambiri.* Gawo lanu loyamba popanga chizolowezi chodzipereka ndikuzindikira zomwe mumayika patsogolo. Chinthu chofunika kwambiri ndi chinthu chimene munthu amaona kuti ndi chofunika kwambiri. Ndi chinthu chimene iye amachita poyamba. Muyenera kusankha kuti ubwenzi wanu ndi Mulungu ndi wofunika kwambiri. Ndipo muyenera kuwona chizolowezi chodzipereka ngati njira yolimbikitsira ubalewo. Kuti muchite izi, muyenera kusamala ndi zomwe zimatchedwa “Chipwilikiti cha changu". Ndiko kuti, musalole zinthu zina za moyo uno zisokoneze makhalidwe amene ali ofunika kwambiri pa moyo wanu.

Monga Mbusa wotanganidwa, mumakumana ndi zofunikira zambiri tsiku lililonse, ntchito zomwe zimafuna nthawi yanu.Ngakhale kuti simunganyalanyaze zofuna zimenezi, muyenera kuphunzira kuziika mu dongosolo lake loyenera. Muyenera kuteteza ubale wanu ndi Mulungu. Ndipo muyenera kusunga ubale umenewo pamwamba pa mndandanda wanu woyamba. Ndicho chimene Yesu anachita. Iye sanalole maudindo ake ambiri kumulepheretsakuyanjana ndi Atate wake wakumwamba. Baibulo limatiuza kuti “Koma Iye anazemba, nanka m’mapululu, nakapemphera” (Luka 5:16). Iye ankadziwa kuti ankafunika nthawi imeneyi yekha ndi Atate wake kuti amuthandize mu utumiki.

Nkhani ya Maria ndi Marita ikusonyezanso mfundo imeneyi. Maria anaika patsogolo kukhala pa mapazi a Yesu ndi kumvetsera kwa Iye akuphunzitsa. Komabe, Marita anatanganidwa kwambiri ndi ntchito imene inafunika kuchitika. Yesu anauza Marita kuti: “Uda nkhawa nuvutika ndi zinthu zambiri, koma chisoweka chinthu chimodzi, pakuti Maria anasankha dera lokoma limenesilidzachotsedwa kwa iye” (Luka 10:41-42). Marita anali atasokonezedwa ndi chipwilikiti cha changu. Komabe, Maria anaika patsogolo chinthu chabwino koposa, chiyanjano ndi Ambuye. Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kuphunzira kuchita zomwezo.

Mwina mungaganize kuti: “Lero sindingathe kuwerenga Baibulo n’kupemphera. Ndili ndi zinthu zambiri zofunika kuchita mwamsanga.” Komabe, ngati mukunena izi lero, ndi tsiku lotsatira, ndi tsiku linalo, mudzagwera mu kachitidwe komwe nkovuta kuthawamo. Koma ngati mudzaona nthawi ya kudzipereka kwanu kwa tsiku ndi tsiku kukhala chopangana ndi Mulungu, ndipo

ngati mudzasunga mokhulupirika choikidwiratu chimenecho, mudzakhala ndi njala ya kukhalapo kwa Mulungu. Mudzayamba kuyandikira nthawi yanu yodzipereka ndi chisangalalo.

2. Kusamalira nthawi. Mfundo yachiwiri imene mbusa wa Chipentekoste akuyenera kuyikonza pakupanga chizolowezi chopemphera ndi kusamalira nthawi. Kusamalira nthawi ndi chizolowezi chokonzekera ndondomeko ya tsiku ndi tsiku kuti muwonetsetse kuti nthawi yoyenerera yaperekedwa pazochitika za tsiku lililonse. Abusa ogwira mtima amazindikira kuti nthawi ndi mphatso yochokera kwa Mulungu, ndipo ayenera kuigwiritsa ntchito bwino. Pokonza tsiku lanu, muyenera kuonetsetsa kuti mukusungira nthawi yokwanira yodzipereka.

Mbusa wina wokhwima maganizo ananena za mmene anakonzera nthawi yake yopemphera. Iye anati: "Ndimapatula nthawi m'mawa uliwonse kaamba ka pemphero lodzipereka ndi phunziro la Baibulo. "Ndimauza anthu anga mmene dongosolo langa liliri. Ndiyeno, ngati panthawiyo munthu wina aitana ndi kunena kwa ine kuti, 'Ndikufuna kukuonani,' ndimawapangitsa kuti adikire mpaka nditamaliza kulambira kwanga. Ndikamaliza, ndimatuluka ndikukumana nawo. Inde, pali zadzidzidzi zomwe ndiyenera kuyankha. Komabe, izi ndizosiyana. Lamulo n'lakuti nthawi imene ndimakhala ndi Mulungu ndiyofunika kuika patsogolo."

3. Kudziletsa. Nkhani yachitatu pakukulitsa chizolowezi champhamvu chodzipereka ndiyo kudziletsa. Ndi ubwino wanji ngati mbusa wa Chipentekoste akhazikitsa zofunika ndikukonzekera nthawi yake koma alibe kudziletsa kofunikira kuti akwaniritse ndi dongosolo lawo? Choncho muyenera kudzilanga kuti musunge zimene munapangana ndi Mulungu tsiku lililonse. Monga Mbusa mulibe amene angakuuzeni kuti, "Yakwana nthawi yopemphera. Ndi nthawi yowerenga Baibulo." Choncho muyenera kudzilanga. Paulo anauza Timoteo kuti woyang'anira, kapena Mbusa, ayenera kukhala wodziletsa (1 Tim. 3:2). Anaphunzitsanso kuti kudziletsa, kapena kudzipatsa mwambo, ndi chipatso cha Mzimu Woyera (Agal. 5:23).

Machitidwe Awiri Odzipereka

Monga tanenera kale m'mutu uno, machitidwe awiri a chizolowezi chodzipereka ndi kupemphera ndi kuphunzira Baibulo. Tiyeni tiyang'ane kwambiri pa chilichonse mwa machitidwewa:

1. Pemphero lodzipereka. Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuphatikiza mapemphero odzipereka mu nthawi yake yodzipereka. Pemphero lodzipereka ndilosiyana ndi pemphero lopempha kapena kupembedzera. M'pemphero lopempha, wofunafunayo akupempha Yehova kuti akwaniritse chosowa m'moyo wake. M'pemphero lopembedzera, iye amapempherera zosowa za ena. Komabe, m'pemphero lodzipereka, wolambirayo akupereka njira yake kwa Mulungu, kufunafuna kuyandikira kwa Iye. Davide anapemphera pemphero lodzipereka pamene anapempha Mulungu kuti, "Mundidziwitse njira zanu, Yehova; Mundiphunzitse mayendedwe anu" (Masalimo 25:4)

Pemphero lodzipereka limaphatikizanso nthawi za kuyimba, kupembedza, ndi kuyamika Mulungu. Nthawi zina kumaphatikizapo kulapa, monga pamene Davide anapemphera kuti, "Pa inu, Inu nokha, ndinachita choipacho pamaso panu.…Mundiyeretse ndi hisope ndipo ndidzayera; munditsuke ndipo ndidzakhala wa mbuu woposa matalala" (Masalimo. 51:4, 7). Mawu a Mulungu amalonjeza kuti, "Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse" (1 Yoh. 1:9).

Pa nthawi yanu yopemphera, mudzafuna kupempherera banja lanu, kuti likhale ndi thanzi labwino lakuthupi ndi lauzimu. Mudzafunanso kupempherera mpingo wanu, kuti Mzimu Woyera akupatseni mphamvu ndikuwongolera zochitika zake, ndi kuti onse omwe ali gawo la mpingo adzazidwe ndi Mzimu. Komanso, mudzafuna kupemphera kuti mpingo ukhale wathanzi komanso kuti mphatso ndi chipatso cha Mzimu zikhalepo mu mpingo.

2. Kuphunzira Baibulo modzipereka. Nthawi yanu yopemphera ikhale ndi kuphunzira Baibulo. Ndikofunika, komabe, kutimumvetsetse kusiyana pakati pa kuphunzira Baibulo modzipereka ndi mwaukadaulo. Kuphunzira Baibulo mwaukatswiri ndi phunziro limene abusa amachita pokonzekera utumiki. Kuphunzira Baibulo kotereku kumachitika akamaphunzira Baibulo kukonzekera ulaliki kapena phunziro la Baibulo. Kwa abusa a Chipentekoste, kuphunzira Baibulo mwaukatswiri ndikofunikira. Komabe, si mtundu wa phunziro la Baibulo limene muyenera kuchita panthawi ya kudzipereka kwanu.

Kuphunzira Baibulo modzipereka kumachitika pamene muwerenga Baibulo kuti mukule mwauzimu. Cholinga chanu si kukonzekera ulaliki koma kumvetsetsa bwino Mawu a Mulungu, ndi kulola mawu a Mulungu kuumba moyo wanu. Cholinga cha kuphunzira Baibulo modzipereka ndikukumana ndi Mulungu

m'Mawu ake. Cholinga chake ndi kumudziwa bwino Mulungu, kuyandikira kwa Khristu komanso kumutumikira mwangwiro. Yobu analankhula za kudzipereka kwake kwa Malemba pamene anati, "Sindinabwerera kusiya malamulo a milomo yake; ndasungitsa mau a pakamwa pake koposa lamulo langalanga" (Yobu 23:12).

Ena apereka njira zinayi zophunzirira Baibulo modzipereka. Chinthu choyamba ndi kuwerenga ndime pang'onopang'ono komanso moganizira. Chinthu chachiwiri ndi kuganizira lembalo, n'kumafunsa mafunso monga akuti, "Kodi Mulungu akundiuza chiyani m'ndimeyi?' komanso "Kodi ndiyenera kuchita chiyani ndi uthenga wa Mulungu umene uli m'ndimeyi?" Chinthu chachitatu ndi kupemphera kuti, "Ambuye, mukufuna kuti ndichite chiyani?" Ndipo chomaliza ndicho kumvera zimene Mulungu wanena m'Mau ake ndi kutsatira mfundo zake.

ZINA ZOKHUDZA KHALIDWE LA KUDZIPEREKA

Pomaliza, tiyeni tione mfundo zina zitatu za mmene mungakulitsire chizolowezi chanu chodzipereka ndi kulimbitsa ubwenzi wanu ndi Mulungu.

Kugwiritsa Ntchito Pemphero la Ambuye

Nthawi zina, mudzafuna kugwiritsa ntchito Pemphero la Ambuye monga chitsogozo m'nthawi za kudzipereka kwanu. Pemphero limeneli likupezeka pa Mateyu 6:9-13. Yesu analipereka kwa ophunzira ake monga chitsanzo, kapena ndondomeko, ya pemphero lamphamvu. Pogwiritsa ntchito pempherori ngati mlozo, gawo lanu lodzipereka lidzayenda motere:

1. *Yambani ndi matamando:* "Atate wathu wa kumwamba, dzina lanu liyeretsedwe" (v. 9). Khalani ndi mphindi zochepa kuyimba ndi kupembedza Mulungu. Mutamandeni chifukwa cha chimene Iye ali, ndipo muthokozeni pa zonse zimene wachita.
2. *Pempherani kuti chifuniro cha Mulungu chichitike*: "Ufumu wanu udze, kufuna kwanu kuchitidwe, monga Kumwamba chomwecho pansi pano" (v. 10). Pempherani kuti Ufumu wa Mulungu ubwere m'miyoyo ya anthu. Pempherani kuti abadwe mwatsopano ndi kuyamba kutsatira Khristu (Yohane 3:3-8). Pempherani kuti achiritsidwe ndi kumasulidwa ku ukapolo wa ziwanda (Mateyu 12:28; Luka 11:20). Apempherereni kuti adzazidwe ndi Mzimu Woyera (Marko 9:1; Machitidwe 1:3-8). Ndipo pemphererani kubwera kwa Yesu posachedwa (Luka 22:18; Chiv. 12:10; 22:20).

3. *Pempherani kwa Mulungu: "*Mutipatse ife lero chakudya chathu chalero" (v. 11). Pemphani Mulungu kuti akupatseni zosowa zanu zonse "monga mwa chuma chake mu ulemerero mwa Khristu Yesu" (Afilipi 4:19). Pempherani pa zosowa za ena.
4. *Pemphani ndi kukhululuka:* "Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa athu" (v. 12). Dzichepetseni pamaso pa Mulungu, kupempha chikhululuko ndi kukhululukira ena.
5. *Pemphani chitsogozo ndi chitetezo cha Mulungu:* "Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo" (v. 13). Pemphani Mulungu kuti akutsogolereni pa moyo wanu ndi utumiki wanu komanso kuti akutetezeni kwa mdierekezi ndi mphamvu zake za ziwanda.

Pemphero Lopitiriza

Kuphatikiza pa kukhala ndi nthawi yodzipereka tsiku ndi tsiku, mbusa wa Pentekoste ayenera kuphunzira "kupemphera kosalekeza" (1 Atesalonika 5:17). Izi, ndithudi, sizikutanthauza kuti muyenera kukhala m'chipinda chopempherera mo tsiku lonse. Zikutanthauza kuti musasiye kupemphera. Muyenera kuphunzira kukhala mu chiyanjano chosalekeza ndi Mulungu. Pamene mukuchita ntchito zanu za tsiku ndi tsiku, pemphero liyenera kukhala pa milomo yanu mosalekeza (Masalimo. 34:1; Aheb. 13:15). Mchitidwewu udzawonjezedwa ngati tsiku lanu liyamba ndi nthawi yodzipereka monga tafotokozera pamwambapa. Pemphero losatha ndilofunika kuti tikhale ndi moyo wogwirizana ndi Mzimu wa Mulungu (Agal. 5:25).

Kulemba

Pomaliza, ndi njira yabwino kwa Mbusa wa Chipentekoste kusunga buku la mapemphero tsiku ndi tsiku. Kabuku ka mapemphero ndi kabuku kamene Mbusa amasungamo zimene zimachitika pa nthawi ya kudzipereka kwake. Mu kabuku kameneko, mukulemba zopempha zomwe munapempha kwa Mulungu, pamodzi ndi mayankho a Mulungu ku zopemphazo. Pamene mukuona kukhulupirika kwa Mulungu poyankha mapemphero anu, chikhulupiriro chanu chidzalimba.

Mufunikiranso kulemba mawu aliwonse kapena malingaliro omwe mungalandire kuchokera kwa Mzimu Woyera. Malingaliro amenewa pambuyo pake angakhale ngati zitsogozo, kukuthandizani kuzindikira chitsogozo cha Mulungu cha moyo wanu ndi utumiki wanu. Kuonjezela apo, mungafune kulemba chidziwitso chilichonse chimene mungamve powerenga Baibulo. Zina mwa

zidziwitso zimenezi pambuyo pake zikhoza kupangidwa kukhala mauthenga wolalikidwa kumpingo. Nthawi zina mudzafuna kubwereza zimene mwalemba m'makabuku kanu, kupempha Mulungu kukhomereza mumtima mwanu zinthu zimene Iye amafuna kuti muzikumbukira.

Kwa abusa a Chipentekoste, chizolowezi chopemphera tsiku ndi tsiku sichosankha; ndichofunika. Chizolowezi choterocho chidzalemeretsa mwamphamvu moyo wake ndi utumiki wake m'njira zambiri. Izi zidzawapatsa chitsogozo ndi mphamvu zauzimu zomwe akufunikira kuti akwaniritse maitanidwe a Mulungu pa moyo wawo.

~ Gawo 5 ~

UTUMIKI OWONEKERA WA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

~ Mutu 16 ~

Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu

Mbusa yemwe sanali wa Chipentekoste amakayikira zenizeni za ubatizo wa Mzimu Woyera. Nthawi zambiri amakayikira zomwe Mzimu amachita. Ndiye tsiku lina, akuwerenga Machitidwe 2 ndi kusinkhasinkha pa zochitika za Tsiku la Pentekoste, iye anapempha ndi kulandira chomwe chinachitika pa Tsiku la Pentekoste. Kenako anachitira umboni kuti: “Patangopita nthawi yochepa kuchokera pamene ndinalandira Mzimu Woyera, kulalikira kwanga kwakhala ndi zotsatirapo zambiri kuposa zaka zonse zam’mbuyomo za kulalikira!”

M'mbiri yakale, kulalikira kwamphamvu, kudzozedwa ndi Mzimu kwakhala chizindikiro cha utumiki wa Chipentekoste. Kuyambira kuchiyambi kwa zaka za zana la makumi awiri, gulu la Chipentekoste latulutsa gulu lankhondo lalikulu la olalikira opatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera, akumalengeza mwachangu uthenga wachipulumutso kwa amitundu.

Mutu uwu ufotokoza za ulaliki wa Chipentekoste. Udzayang'ana pa udindo wa Mzimu Woyera pakudzoza mlaliki. Udzaperekanso malingaliro okonzekera ulaliki ndi kalalikidwe kake.

KULALIKIRA KWA PENTEKOSTE

Yesu analamula ophunzira ake kuti: “Mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse” (Marko 16:15). Kulalikira ndiko

kulengeza kwachangu kwa Mawu a Mulungu ndi cholinga chokopa anthu kutsatira Khristu ndi kuchita chifuniro Chake. Ndi mutu wodziwika bwino mu Chipangano Chatsopano pomwe mawu ena *olalikira* kapena *kulengeza* amapezeka pafupifupi kokwana ka 150. Kukhoza kulalikira mogwira mtima, mauthenga odzodzedwa ndi Mzimu ndi udindo waukulu wa mbusa aliyense wa Chipentekoste.

Buku la Machitidwe ngati Chitsanzo

Mapentekoste amakhulupirira kuti kulalikira kwa atumwi ndi anthu ena m'buku la Machitidwe kunayenera kukhala chitsanzo kwa alaliki masiku ano. Mu Machitidwe, Luka akulemba zomwe zili mu maulaliki angapo olalikidwa ndi atumwi ndi alaliki ena (monga Petro: Machitidwe 2:14-40; 3:12-26; 10:28-47; Stefano: Machitidwe 7:1-53; Paulo: Machitidwe 13:16-41; 17:22-31). Malo ochuluka amene Luka anapereka ku maulaliki amenewa a m'buku la Machitidweakusonyeza kufunika kwake. Iye ankafuna kuti owerenga ake adziwe mmene atumwi ankalalikirira kuti nawonso azichita chimodzimodzi.

Kuyang'ana mosamalitsa maulaliki a m'buku la Machitidwekumasonyeza zinthu zisanu zofunika kwambiri za ulaliki wa atumwi:

1. *Kukhazikika pa Yesu*. Umunthu ndi ntchito ya Khristu ndi phata lenileni la uthenga uliwonse wolalikidwa mu Machitidwe. Alalikia Chipangano Chatsopano analengeza mosalekeza kuti Yesu anali kukwaniritsidwa kwa ulosi wa m'Chipangano Chakale, ndi kuti Iye anali njira yokhayo ya chipulumutso (onani Machitidwe 2:22-24, 30-32; 3:13-20; 4:10-12) 5:30-31; 8:5; ndi ena).
2. *Amakhazikika pa Malemba*. Alaliki a m'buku la Machitidwe a Atumwi nthawi zonse ankalimbikitsa zonena zawo za m'Malemba (onani Machitidwe 2:17-21; 3:22-23; 4:11, 25-26; ndi ena).
3. *Kudzozedwa ndi Mzimu* Woyera. Alaliki a m'buku la Machitidwe a Atumwi anadzazidwa, motero anadzozedwa ndi Mzimu Woyera (onani Machitidwe 2:4, 14; 4:8; ndi ena).
4. *Chitsimikizo chauzimu*. Mu Machitidwe, kulengeza kwa Uthenga Wabwino nthawi zambiri kunkatsagana ndi zizindikiro zotsimikizira ndi zodabwitsa (fanizilani Machitidwe 3:1-8; 8:4-7; 14:8-10; ndi ena).
5. *Kuitana ku kulapa ndi chikhulupiriro*. Alaliki a m'buku la Machitidwe a Atumwi amamaliza maulaliki awo ndi mayitanidwe a kulapa ndi chikhulupiriro (onani Machitidwe 2:38; 3:19; 8:22; ndi ena).

Makhalidwe omwewa ayenera kukhala pamtima pa ulaliki wa Chipentekoste mu Afirika lero. Mungachite bwino kuloweza mndandanda umenewu ndi kuugwiritsa ntchito monga muyezo wothandizira utumiki wanu wolalikira.

KUDZOZA KWA MZIMU WOYERA

M'chipangano Chakale, aneneri, ansembe, ndi mafumu anadzozedwa ndi mafuta pamene anaikidwa pa udindo (Eksodo. 28:41; 1 Samuele 9:16; 16:11-13; 1 Mafumu 1:34; 19:16). Kudzozedwa kumeneku kunatumikira monga chizindikiro cha kuitanidwa kwawo, ndipo kunaimira ulamuliro wawo wopatsidwa ndi Mulungu wa kugwira ntchito m'maudindo awo. Zinasonyezanso kupezeka kwa Mzimu wa Mulungu pa iwo kuti athe kugwira ntchito za udindo wawo (Yes. 61:1-2).

Monga tanenera kale, mbali imodzi ya ulaliki m'buku la Machitidwe ndi yakuti alaliki anadzozedwa ndi Mzimu Woyera. Tiyeni tiwone bwinobwino lingaliro limeneli.

Utumiki Wodzozedwa wa Yesu

Yesu anayamba utumiki wake mwa kulengeza kuti: "Mzimu wa Ambuye uli pa ine, chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino" (Luka 4:18). Motero analongosola kudzoza kwa Mzimu monga Mzimu kukhala pa Iye. Anagwiritsa ntchito mauwa kufotokoza za kugwira ntchito kwamphamvu kwa Mzimu Woyera mwa Iye ndi kudzera mwa Iye, kumupangitsa Iye kuchita utumiki wake waumesiya.

Utumiki Wodzozedwa wa Atumwi

N'chimodzimodzinso ndi ophunzira 120 pa Tsiku la Pentekoste. Poyamba, Mzimu anadza pa iwo (Machitidwe 2:3). Ndipo Iyeanawadzaza iwo. Ndipo potsiriza, Iye anayamba kulankhulakupyolera mwa iwo (Machitidwe 4, 14). Zonsezi zinachitika m'kukwaniritsidwa kwa lonjezo la Yesu pa Machitidwe 1:8: "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga…kufikira malekezero ake a dziko."

Choncho, kudzozedwa ndiko kudzazidwa ndi kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Monga momwe Mzimu anadza pa Yesu ndi ophunzira oyambirira, kuwadzoza ku utumiki, Mzimu adzabwera pa wophunzira wodzipereka lero, kumudzoza iye ku utumiki.

Kudzoza Kufotokozeredwa

Kudzoza ndiko kugwira ntchito kwamphamvu kwa Mzimu Woyera mkati, kupitiriza, ndi kupyolera mwa anthu amene adzipereka kwathunthu kwa Mulungu. Ndi kupezeka kwa Mulungu kowonekera kumene kumabwera pa wophunzira wodzazidwa ndi Mzimu, kumupangitsa iye kutumikira ndi mphamvu yowonjezereka ndi kuchitapo kanthu.

M'buku la Machitidwe, mawu *odzazidwa* ndi *odzala* ndi Mzimu Woyera nthawi zina amagwiritsidwa ntchito kufotokoza kudzoza kwa Mzimu. Mawuwa, odzazidwa ndi Mzimu Woyera, amafotokoza za kubwera kwa Mzimu, kudzadza, ndi kudzoza munthu kuchita ndi kulankhula ndi mphamvu ndi ulamuliro (Machitidwe 4:8, 31; 13:9-12). Mawuwa, odzala ndi Mzimu Woyera, amafotokoza za kudzozedwa kopitilira muyeso kwa Mzimu Woyera (Machitidwe 6:3, 5; 7:55). Uku kungakhale "kudzoza komwe kumatsalira" konenedwa ndi Yohane (1 Yohane 2:27). Kudzoza kumakhalabe pa ife ngati tikhala mwa Khristu (Yohane 15:4-7). Kulekanitsidwa ku uchimo ndi chinthu chofunikira kuti kudzoza kukhalebe (Yohane 14:15-16). Kudzoza kumeneku kuyenera kukhala kofunikira m'moyo wa Mbusa aliyense wa Chipentekoste.

Ulaliki Wodzozedwa

Ulaliki wodzozedwa ndi Mzimu suyenera kusokonezedwa ndi kulankhula mwaluso, chikoka chachibadwa, kapena kuthekera kwa kukopa khamu la anthu. Komanso siziyenera kusokonezedwa ndi ulaliki wachidwi. Ngakhale ulaliki wodzozedwa ndi Mzimu ukhoza kusonyeza makhalidwe awa, ndi zambiri. Kulalikira kodzozedwa ndi Mzimu ndiko kulalikira kodzazidwa ndi Mzimu. Ndi mtundu wa ulaliki umene Yesu ndi atumwi anatsanzira.

Luka akuchitira chitsanzo chowonadi chimenechi ndi nkhani ya Apolo. Iye akufotokoza kuti: "Apolo…munthu wolankhula mwanzeru; ndipo anali wamphamvu m'malembo. Iyeyo anaphunzitsidwa m'njira ya Ambuye; pokhala nao mzimu wachangu, ananena ndi kuphunzitsa mosamalira zinthu za Yesu" (Machitidwe 18:24-25). Chotero Apolo anali mlaliki waluso ndi waluntha. Komabe iye "anadziwa ubatizo wa Yohane wokha" (v. 25). Iye analibe chomuchitikira cha Pentekoste. Komabe, Prisila ndi Akwila "atamufotokozera momveka bwino njira ya Mulungu," mwachionekere anadzazidwa ndi mzimu woyera. Kenako anapita ku Akaya kumene "iye anathangata ndithu iwo akukhulupirira mwa chisomo" (v. 27).

Yesu nkudzodzedwa kwake analalikira ndi kuphunzitsa kuti: "Mawu amene ndalankhula ndi inu ndiwo mzimu, ndi moyo" (Yoh. 6:63). Baibulo limafotokoza ulaliki wa atumwi kuti: "Atumwi anachita umboni ndi mphamvu yaikulu za kuuka kwa Ambuye Yesu; ndipo panali chisomo chachikulu pa iwo onse" (Mach. 4:33). Mawu akuti, *panali chisomo chachikulu pa iwo onse*, akufotokoza bwino za kudzoza kwa Mzimu Woyera. Mu Machitidwe, kudzoza kwa Mzimu pa mlaliki kunakhudza kwambiri iwo amene anamvetsera (Mach. 2: 4, 14 ndi 1 Ako. 2: 4; Mach. 2: 37 ndi 1 Ako. 2: 5).

Paulo analankhula za kulalikira kwake kodzozedwa ndi Mzimu mu makalata ake. Iye anakumbutsa Akhristu a ku Korinto mmene iye analalikira uthenga wabwino poyamba. Iye analemba kuti: "Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhale ndi mau okopa a nzeru, koma m'chionetsero cha Mzimu ndi cha mphamvu" (1 Ako. 2:4-5. Iye anafotokoza utumiki wake kwa okhulupirira a ku Aroma: "Mu mphamvu ya zizindikiro ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya Mzimu Woyera … ndinakwanitsa Uthenga Wabwino wa Khristu" (Aroma 15:19). Iye anakumbutsa okhulupirira a ku Atesalonika kuti: "Uthenga Wabwino wathu sunadze kwa inu, m'mau mokha, komatunso mu mphamvu, ndi mwa Mzimu Woyera, ndi m'kuchuluka kwakukulu" (1 Ate. 1:5).

Mzimu Woyera ndi wokonzeka kudzoza ulaliki wathu masiku ano monga mmene anadzozera Yesu ndi atumwi ake m'nthawi ya atumwi. Koma kodi kudzoza kumachokera kuti, ndipo tingatani kuti tichite zimenezi?

GWERO LA KUDZOZA

Kuti athe kulalikira ndi kudzoza kwa Mzimu, mbusa wa Chipentekoste ayenera kudziwa gwero lake. Magwero a kudzoza ndiko kupezeka ndi kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Ndi kupezeka kwa Mzimu mkati ndi pa moyo wa mlaliki (Yoh. 14:17; Mach. 1:8). Mphamvu iyi ya Mzimu Woyera imalandiridwa pamene munthu wabatizidwandikudzazidwa ndi Mzimu Woyera (Mach. 2:4). Kudzoza kumakhalabe pamene munthu akuyenda "motsatana ndi Mzimu" (Agal. 5:25). Choonadi chimenechi chimaonekera mu utumiki wa Yesu ndi atumwi ake.

Gwero La Kudzodza Kwa Yesu

Yesu anatsimikizira kuti gwero la kudzoza kwake anali Mzimu wa Ambuye (Luka 4:18). Ngakhale kuti analidi Mwana wa Mulungu wobadwa m'thupi, anasankha kudzikhuthula yekha ku mphamvu yake yaumulungu ndi mwayi wake

ndi kuchita utumiki Wake mu mphamvu ya Mzimu (Afilipi 2:5-8). Motero utumiki wa Yesu wodzozedwa ndi mzimu ndi chitsanzo kwa onse amene angamutsatire.

Yesu sanayambe utumiki wake mpaka atadzozedwa ndi Mzimu. Ubatizo wake wa Mzimu unachitika atangobatizidwa ndi Yohane m'madzi. Baibulo limati: "Iye [Yesu] anali kupemphera, ndipo kuthambo kunatseguka, ndipo Mzimu Woyera anatsika ndi maonekedwe a thupi ngati nkhunda, nadza pa Iye" (Luka 3:21-22). Kenako Yesu "anayamba ntchito yake" (v. 23). Anayamba kuyenda ndi kutumikira mu mphamvu ya Mzimu (Luka 4:1, 14). Iye analengeza kuti: "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino" (Luka 4:18). Pambuyo pake, anthu atamva Yesu akulankhula, "[a]nazizwa ndi mawu achisomo akutuluka m'kamwa mwake" (v. 22). Ndipo anadabwa "chifukwa mawu ake anali ndi ulamuliro" (v. 32; onaninso Mateyu 7:28 29).

Gwero la Kudzoza kwa Atumwi

Monga momwe Mzimu Woyera anali gwero la utumiki wodzozedwa wa Yesu, Iye analinso gwero la utumiki wodzozedwa wa atumwi. Monga Yesu, atumwi anabatizidwa koyamba ndi Mzimu Woyera. Kenako anayamba kulalikira ndi mphamvu.

Petro ayenera kuti ndi chitsanzo chabwino kwambiri pa nkhani ya uzimu imeneyi. Pentekoste isanafike, iye ankaopa kuvomereza Yesu kwa mtsikana wantchito (Mat. 26:69-72). Komabe, atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, analalikira ndi mphamvu, ndipo mawu ake anakhudza kwambiri omvera ake (Mach. 2:37). Chifukwa cha ichi, anthu zikwi zitatu anabwera kwa Khristu. Izi zikubwerezedwa kangapo mu Machitidwe (4:8, 31-33).

Kudzozedwa komweko kumene kunali pa Yesu ndi atumwikumene kunkawathandiza kulalikira ndi mphamvu kukupezekanso kwa ife masiku ano.

KUKUMANA NDI KUDZOZA

Mafunso amabuka, "Kodi munthu angalandire bwanji kudzozedwa kwa Mzimu Woyera lero? Kodi kudzoza kumalandiridwa bwanji? Kodi kumaonekera bwanji mu utumiki? Kodi kungasungidwe bwanji?"

Kulandira Kudzoza

Kudzozedwa kumalandiridwa lero lino monga momwe analandirira Yesu ndi ophunzira oyambirira. Zimalandiridwa poyamba pamene munthu wabatizidwa ndi Mzimu Woyera. Monga tafotokozera pamwambapa, Yesu analandira Mzimu Woyera pa ubatizo wake. Kenako anayamba kutumikira ndi mphamvu. Ndi momwemonso mmene zinalili ndi ophunzira ake. Iwo anayamba kulandira Mzimu pa Pentekoste, ndipo monga Yesu, iwonso anayamba kutumikira ndi mphamvu.

Yesu anapereka malangizo omveka bwino okhudza mmenemunthu angalandirire Mzimu. Iye anauza ophunzira ake kuti: "Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akumpempha Iye!" (Luka 11:13). Iye anafotokoza kuti: "Pemphani, ndipo adzakupatsani; funani, ndipo mudzapeza; gogodani ndipo adzakutsegulirani. Pakuti yense wakupempha alandira; ndi wofunayo apeza; ndi iye amene agogoda adzamtsegulira" (vv. 9-10). Mzimu amalandiridwa mwa kupempha ndi chikhulupiriro (v. 9), kulandira ndi chikhulupiriro (v. 10 ndi Marko 11: 24), ndi kulankhula ndi chikhulupiriro (Machitidwe 2: 4).[1]

Kuwonetsera Kudzoza

Kudzoza komwe kumalandiridwa pa ubatizo wa Mzimu kumawonekera mu utumiki makamaka kudzera mu machitidwe a mphatso zauzimu. Zowonadi, kulalikira kodzozedwa ndi Mzimu ndiko chisonyezero cha mphatso ya ulosi. Ndi mawu otsogozedwa ndi Mzimu, odzozedwa ndi Mzimu. Kulalikira kodzozedwa ndi mzimu kungaphatikizeponso kusonyezedwa kwa mphatso za mavumbulutso monga mawu achidziwitso ndi mawu anzeru. Kuphatikiza apo, kulalikira kodzozedwa ndi Mzimu nthawi zambiri kumatsagana ndi mawonetseredwe a mphatso yamphamvu, monga zidachitikira ndi Paulo ku Listara (Mach. 14: 8-10).[2]

Mutha kupeza kudzoza pakufunsa, ndikuyankha mwachikhulupiriro, kupezeka kwa Mzimu Woyera. Pamene mukuyandikira guwa, muyenera kupemphera, "O Mzimu Woyera, bwerani tsopano ndipo mundidzoze kuti nditumikire Mawu anu." Muyenera kusuntha ndi chikhulupiriro, mukukhulupirira kuti Mulungu wamva pemphero lanu. Mukazindikira kupezeka kwa Mzimu,

[1] Zambiri zikunenedwa potambasulira za kulandira Mzimu Woyera mu mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

[2] Onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

yankhani ndi chikhulupiriro, kugonjera ku chitsogozo chake ndi kumudalira Iye kuti akuthandizeni ndi kukupatsani mphamvu mkulalikira kwanu.

Kusunga Kudzodza

Kudzoza kumasungidwa pakukhala ndi kuyenda mu Mzimu (Agal. 5:25). Mayendedwe odzazidwa ndi Mzimu ndi moyo wodzipereka kwa Mulungu ndi ntchito yake. Pemphero,kuphatikizirapo kupemphera mwa mzimu, ndi chinthu chofunikira kwambiri pakusunga kudzoza (Aroma 8:26-27; 1 Ate. 5:17).

KAKONZEKEREDWE NDI KAPEREKEDWE KA ULALIKI KODZOZEDWA

Mbusa aliyense wa Chipentekoste amene akufuna kukhala mlaliki wogwira mtima, wodzozedwa ndi Mzimu adzafunika kudzipereka pakukonzekera ndi kupereka ulaliki. Ayenera kuonetsetsa kuti Mzimu Woyera alipo, akudzoza ndi kutsogolera ntchito iliyonse.

Kukonzekera Uthenga

Kuyang'ana mosamalitsa ulaliki wa m'buku la Machitidwe kumasonyeza mfundo ziwiri zofunika kwambiri za choonadi: Mauthenga a atumwi anadzazidwa ndi Malemba, ndipo anadzozedwa ndi Mzimu Woyera. Alaliki a m'buku la Machitidwe anasonyeza kuti ankadziwa bwino Malemba. Nthawi zambiri ankagwira mawu a m'Malemba mu mauthenga awo. Mwachitsanzo, ulaliki wa Petro wa Pentekoste uli ndi mawu anayi a Chipangano Chakale (fanizilani Mach. 2:16-21, 25-28, 31, 34-35). Mofananamo, uthenga wa Stefano ku Bwalo Lalikulu la Ayuda uli ndi mawu asanu ndi atatu wotengedwa m'Malemba (Machitidwe 7:3, 6-7, 28, 32-35, 37, 40, 42-43, 49). Maulaliki ena mu Machitidwe amatsatira ndondomeko yomweyi. Alaliki oyambirira amenewa anamvetsa Malemba, ndipo anazika mauthenga awo pa kamvedwe kameneko.

Abusa a Chipentekoste mu Afirika lero ayenera kuchita chimodzimodzi. Mofanana ndi atumwi athu, tiyenera kulalikira molimba m'Malemba. Kuti tichite zimenezi, tiyenera kudzipereka pakusanthula malemba modekha. Tiyenera kukhala ndi nthawi yokwanira mlungu uliwonse yowerenga Baibulo mozama ndi kukonzekera ulaliki. Pamene tikukonzekera, tiyenera kuyang'ana kwa Mzimu Woyera kuti adzoze ndi kulimbikitsa maganizo athu, pozindikira kuti kudzoza kwa Mzimu Woyera sikuletsa kukonzekera; zimangowonjezera.

Komanso mu Machitidwe a Atumwi alaliki anapemphera moyembekezera kudzazidwa ndi kudzozedwa ndi Mzimu Woyera. Buku la Machitidwe limagwirizanitsa kubwera kwa Mzimu Woyera ndi pemphero. Mwachitsanzo, ophunzira anali kupemphera kutsanulidwa pa Pentekoste kusanachitike (Machitidwe 1:14; 2:1-4); okhulupirira a ku Yerusalemu anali kupemphera asanatsanulidwe kachiwiri kwa Mzimu mu mzinda (Machitidwe 4:23-31); ndipo Paulo ndi Hananiya anali kupemphera Paulo asanadzazidwe ndi Mzimu (Machitidwe 9:5, 10-15). Zitsanzo zina zikhoza kutchulidwa.

Ife abusa aChipentekoste amene tikufuna kuti Mzimu Woyera atidzoze kulalikira kwathu tiyenera kudzipereka tokha ku pemphero. Pemphero lodzipereka lotero lidzatsimikizira kudzoza kwa Mzimu, kukhudza kwambiri zomwe zili mkati ndi kuperekedwe ka maulaliki athu.

Kupereka Uthenga

Cholinga cha ulaliki si kukopa omvera koma kukulitsa kumvetsetsa kwa anthu uthengawo. Chilichonse chonenedwa kapena kuchitidwa chikhale ndi cholinga chotsogolera anthu kuti akumane ndi Mulungu. Njira kapena machitidwe aliwonse omwe amathandizira kuti akwaniritse cholingachi ayenera kutsatiridwa. Chilichonse chomwe chimasokoneza cholingacho chiyenera kutayidwa.

Chotero, monga alaliki aChipentekoste, khalidwe lathu liyenera kukhala loona ndi losakhudzidwa. Tiyenera kupewa kung'ung'udza, kukuwa, kuyenda mopanda cholinga, ndiponso kugwedeza manja mwa mavuvu. M'malo mwake, pamene tigwiritsa ntchito manja popereka uthenga tisachite mwa chisawawa komanso kubwerezabwereza. Mayendedwe athu azichokera mkati otsogozedwa ndi Mzimu komanso ndi zomwe zili mu uthenga. Ngati tingagwirizane ndi uthengawo m'maganizo ndi m'zichitochito, manja adzatsatira moyenera ulaliki wathu.

Kuyitanira kugome ndikofunikira kwambiri. Munthawi yovuta iyi ya ulaliki, ndikofunikira kuti mlaliki atsogoleredwe ndi Mzimu Woyera. Kuyitanira kugome si nthawi yofotokozera malingaliro atsopano mu uthenga. Mlaliki ayenera kukhala watcheru ndipo asamapite patali. M'malomwake, ayenera kukhala pa mfundo ndi kupereka malangizo omveka bwino pa zimene akupempha anthu kuti achite.

Abusa a Chipentekoste ndi apadera pakati pa alaliki chifukwa timadalira ndi kufunafuna kudzoza kwa Mzimu Woyera pa kulalikira kwathu. Pochita izi, tikufuna kutsatira chitsanzo cha Yesu ndi alaliki a Chipangano Chatsopano. “Ambuye, dzazani ndi kundidzoza kuti ndichite utumiki” liyenera kukhala pemphero lathu lolimbikira.

~ Mutu 17 ~

Kuphunzitsa Kwabwino

Anthu anga aonongeka chifukwa cha kusadziwa" (Hoseya 4:6). Mawu a Mulungu amenewa ananenedwa kwa ansembe a Israele kudzera mwa mneneri Hoseya. Chifukwa chakuti atsogoleri auzimu amenewa analephera kuphunzitsa anthu a Mulungu choonadi, anakhulupirira mabodza. Chifukwa cha zimenezi, iwo anasochera kwambiri mu uchimo. Mneneriyo anafotokoza mkhalidwe wawo womvetsa chisoni kuti: "Palibe choonadi, kapena chifundo, kapena kudziwa Mulungu m'dziko. Koma kulumbira, ndi kunama, ndi kupha, ndi kuba, ndi kuchita chigololo" (vv. 1-2).

N'zomvetsa chisoni kuti Akhristu ambiri a Chipentekoste ku Afirika kuno akukumana ndi vuto ngati limeneli. Iwo samvetsa bwino Mawu a Mulungu. Chotero, kukula kwawo kwauzimu kwakwinimbira. Chifukwa cha zimenezi, ambiri akuonongedwa mosavuta ndi aphunzitsi onyenga. Monga Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste, muyenera kuonetsetsa kuti mkhalidwe woterewu mulibe mu mpingo uliwonse umene mwaitanidwa kukhala Mbusa.

UDINDO WA MBUSA

Mbusa aliyense wa Chipentekoste ali ndi udindo wodyetsa nkhosa za Mulungu. Pamsonkhano wake womaliza ndi abusa a mpingo wa ku Aefeso, Paulo anawalimbikitsa kuti: "Tadzichenjerani nokha, ndi gulu lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyang'anira" (Machitidwe 20:28). Kenako analamula

abusawo kuti: “Muwete [kapena kuti “dyetsani”] Mpingo wa Mulungu, umene anaugula ndi mwazi Iye yekha.” Paulo ankadziwa kuti pophunzitsa anthu a Mulungu Mawu a Mulungu, abusa a ku Aefeso akanawathandiza kukhala olimba mwauzimu. Zimenezi zikanawakonzekeretsa kukana “mimbulu yosautsa” imene posachedwapa idzalowe m’mpingo, kupotoza chowonadi, ndi kufuna kukopa anthu kuti achoke kwa Khristu (vv. 29-30).

Kuphunzitsa kuli pachimake pa tanthauzo la kukhala Mbusa wa Chipentekoste. Paulo analemba za mphatso zisanu za utumiki zimene Khristu wapereka ku mpingo: “Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi; ndi ena aneneri; ndi ena alaliki, ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi, kuti akonzekere oyera mtima ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu” (Aefeso. 4:11-12).

Taonani momwe, mu ndime iyi, Paulo akuphatikiza mphatso ziwiri zomalizira za utumiki umodzi. [Mukatanthauziridwe kena ka Baibulo] M’malo monena kuti “ndi ena abusa ndi ena aphunzitsi,” monga mmene anachitira ndi mphatso zitatu zoyambirira, Paulo anangoti “abusa ndi aphunzitsi.” Chifukwa cha zimenezi, akatswiri ena amanena kuti mphatso imeneyi ndi “Mbusa-mphunzitsi.” Mfundo yake ndi iyi: Kuti mwamuna kapena mkazi akhale Mbusa, ayeneranso kukhala mphunzitsi. Amene Mulungu amamuitana ku ubusa, amamupatsa mphatso yophunzitsa.

Kuti musamalire bwino nkhosa, muyenera kukhala okhoza kudyetsa bwino anthu a Mulungu, kuwadyetsa Mawu a Mulungu. Baibulo limayerekezera Mawu a Mulungu ndi zakudya zopatsa thanzi monga mkate (Mateyu. 4:4), mkaka (1 Petro. 2:2), ndi chakudya chotafuna (Ahebri. 5:12-14). Mbusa aliyense amene amalephera kudyetsa anthu ake Mawu a Mulungu ndi Mbusa wosakhulupirika, ndipo Mulungu adzamuimba mlandu chifukwa cha kulephera kumeneku (Yakobo 3:1; Ezekiele 34:16).

Komabe, ngati muphunzitsa anthu Mawu a Mulungu mokhulupirika, mudzalemekezedwa ndi Mulungu (Mat. 24:45-47). Koposa zonse, anthu a Mulungu adzalimbikitsidwa. Iwo “sadzakhalanso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengekatengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjerera kukatsata chinyengo cha kusocheretsa, koma ndi kuchita zoona mwachikondi tikakule m’zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu, ndiye Khristu” (Aef. 4:14-15) Pamenepa, iwo amakula kukhala thupi lokhwima la iye amene ali mutu.

Kupanga Ophunzira

Yesu analamulira mpingo wake, "Pitani, phunzitsani anthu a mitundu yonse" (Mat. 28:19). Iye anali kuwauza kuti ayenera kuchita ndi ena zimene Iye anawachitira. Yesu anayenda ndi ophunzira ake, anawaphunzitsa choonadi, ndiponso anawasonyeza mmeneangakhalire ndi moyo. Monga abusa a Chipentekoste, tiyenera kuchita chimodzimodzi ndi mamembala a mpingo wathu.Sikokwanira kutembenuza anthu, tiyenera kupanga ophunzira. Wophunzira ndi wotsatira wodzipereka wa Khristu. Iye ndi amene amakhala pa mapazi a Yesu ndi kuphunzira kwa Iye. Sikuti tiyenera kokha kuitana anthu kuti atsatire Khristu, tiyenera "kuwaphunzitsa kumvera" malamulo ake onse (v. 20).

Kulalikira ndi kuphunzitsa

Abusa ambiri a Chipentekoste ku Afirika amadziona ngati alaliki, koma samadziona ngati aphunzitsi. Monga Mbusa, komabe, Mulungu wakuitanani kuti mukhale zonse ziwiri. Muyenera kukhalanso mlaliki waluso komanso mphunzitsi wogwira mtima. Kuti mumvetse bwino udindo wanu monga mphunzitsi wa anthu a Mulungu, muyenera kudziwa kusiyana pakati pa kulalikira ndi kuphunzitsa.

Baibulo limasiyanitsa momveka bwino pakati pa ntchito ziwirizi. Mwachitsanzo, Baibulo limanena kuti Yesu "anayenda m'Galileya monse, *naphunzitsa* m'masunagoge mwawo, *kulalikira* uthenga wabwino wa ufumu" (Mateyu. 4:23, kutsindika kwawonjezeredwa). Limanena za Paulo ndi Barnaba kuti "anatsalira ku Antiokeya, kumene iwo ndi ena ambiri *anaphunzitsa* ndi *kulalikira* mawu aAmbuye" (Machitidwe 15:35, kutsindika kwawonjezeredwa). Paulo analimbikitsa Timoteyo, Mbusa wa mpingo wa ku Aefeso kuti: "Kufikira ndidza Ine, ukhale wodzipereka pa kuwerenga Malemba, *kulalikira*, ndi *kuphunzitsa*" (1 Timoteo. 4:13, kutsindika kwawonjezeredwa). Nanga pali kusiyana kotani pakati pa kulalikira ndi kuphunzitsa?

Pamtima pake, kulalikira ndiko kulengeza poyera uthenga wabwino ndi cholinga choyitanira anthu ku chikhulupiriro mwa Khristu. Kuphunzitsa ndi kufotokoza tanthauzo la kukhala moyo mwa Khristu. Kulalikira ndi kulengeza; kuphunzitsa ndi kulangiza. Kulalikira ndi kupanga chilengezo; kuphunzitsa ndi kupanga ophunzira. Mlaliki akuyitana oyendayenda ku chikhulupiriro mwa Khristu; Mphunzitsi amawafotokozera njira za Ambuye. Cholinga cha mphunzitsi ndi kusonyeza anthu a Mulungu mmene angamutumikire mwangwiro. Monga Mbusa ndi mphunzitsi, muyenera kufotokoza Malemba mosamala kwa anthu a

Mulungu. Muyenera kuwapatsa chidziwitso ndi zidziwitso zomwe akufunikira kuti agwiritse ntchito mawu omwe amva.

Kutsatira Chitsanzo cha Yesu

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuyesetsa kutsatira chitsanzo cha Yesu, mphunzitsi woposa onse amene anakhalako. Nthawi zambiri Yesu ankadzitchula kuti "Mphunzitsi" (Mat. 26:18; Yoh. 13:13-14). Ena anachitanso chimodzimodzi (monga Mateyu. 8:19; 12:38; Luka 10:25; Yoh. 11:28). Mauthenga Abwino nthawi zambiri amalankhula za utumiki wa Yesu wophunzitsa (Mwachitsanzo, Marko 1:21-22; Luka 4:31-32). Ndipo ndime zazitali za m'Malemba zaperekedwa ku ziphunzitso Zake. Ndimezizikuphatikizapo Chiphunzitso cha paphiri (Mat. 5-7), Chiphunzitso cha pansi pa phiri la Azitona (Mat. 24-25), ndi Chiphunzitso cha M'chipinda Chapamwamba (Yoh. 14-16). Ngati Yesu ankaona utumiki wake wophunzitsa kukhala wofunika kwambiri, ifenso tiyenera kutero masiku ano.

Tinganene zambiri za mmene Yesu anakwaniritsira utumiki Wake wa kuphunzitsa. Mabuku alembedwa onena za njira zake zophunzitsira. Mbali zitatu za njira Yake yophunzitsira ziyenera kutchulidwa:

1. Anaphunzitsa ndi ulamuliro. Baibulo limanena za Yesu kuti: "Ndipo anazizwa ndi chiphunzitso chake; pakuti anaphunzitsa monga mwini mphamvu, si monga alembi" (Marko 1:22). Yesuanaphunzitsa mwaulamuliro chifukwa anatumidwa ndi Mulungu, ndiponso chifukwa chakuti analankhula mawu amene Mulungu anam'patsa. Iye anachitira umboni, "Sindichita kanthu kwa Ine ndekha, koma ndilankhula monga anandiphunzitsa Atate, ndilankhula izi" (Yoh. 8:28). Iye anachitira umboni. Kuti muphunzitse ndi ulamuliro, monga mmene Yesu anachitira, inunso muyenera kuphunzitsa Mawu a Mulungu mokhulupirika.

2. Anaphunzitsa mwachikondi. Yesu ankakonda kwambiri anthu amene ankawaphunzitsa. Kuphunzitsa kwake kunali, kwenikweni, kuchulukira kwa chikondi chake pa anthu. Nthawi ina, Yesu anakumana ndi khamu lalikulu la anthu otopa ndi anjala. Iye atawaona "[a]nagwidwa ndi chifundo, chifukwa anali ngati nkhosa zopanda mbusa." Kenako, chifukwa cha chikondi chake chachikulu pa iwo, "anayamba kuwaphunzitsa zinthu zambiri" (Marko 6:34). Kenako anawadyetsa chakudya chakuthupi (vv. 35-44). Koma choyamba, Iye anatumikira ku chosowa chawo chachikulu ndi kuwadyetsa iwo Mawu a Mulungu.

Pa nthawi ina, Yesu anakumana ndi ophunzira ake m'chipinda chapamwamba. Baibulo limati: "Podziwa kuti nthawi yake idzadza yakuchoka kutuluka m'dziko lino lapansi, kunka kwa Atate, m'mene anakonda ake a Iye yekha a m'dziko lapansi, anawakonda kufikira chimaliziro" (Yoh. 13:1). Kachiwirinso, chifukwa cha chikondi chake chakuya kwa iwo, ndi kwa awo amene iwo eniwo adzatsogolera posachedwapa, anawaphunzitsa phunziro lamphamvu pa utsogoleri wa utumiki (vv. 2-17).

Pazochitika zonsezi, chikondi cha Yesu pa anthuchinamukakamiza kuwaphunzitsa. Momwemonso, ngati Mbusa wa Chipentekoste muyenera kukonda iwo omwe mudayitanidwira kuti muwatsogolere. Ndipo chikondi chimenechi chiyenera kukulimbikitsani kuwaphunzitsa Mawu a Mulungu mokhulupirika. Popanda chikondi choterocho kwa anthu anu, mawu anu angakhale "mkuwa woomba, kapena nguli yolira" (1 Ako.13:1).

3. Anaphunzitsa mu mphamvu ya Mzimu. Nthawi ina Yesu anafotokozera ophunzira ake za utumiki wake wophunzitsa. Iye anati: "Mawu amene ndalankhula ndi inu ndiwo mzimu, ndi moyo" (Yoh. 6:63). Mawu a Yesu anali odzala ndi Mzimu ndi moyo chifukwa Iye mwiniyo anali wodzala ndi Mzimu ndi moyo. Anayamba utumiki wake pakudzozedwa ndi Mzimu Woyera (Luka 3:21-22; 4:18-19). Kenako adachita utumiki wake wophunzitsa mu mphamvu ya Mzimu (Luka 4:14-15).

Yesu anaphunzitsa, osati ndi mawu okha, koma ndi mawonetseredwe a mphamvu ya Mzimu (Luka 5:17). Mawu ake anali odzala ndi mphamvu ya Mzimu kotero kuti, pamene Iye anali kuphunzitsa, ziwanda zinafuula, "Tili ndi chiyani ife ndi Inu Yesu wa ku Nazarete? Kodi mwadza kudzationonga? Ndikudziwani ndinu Woyerayo wa Mulungu (Marko 1:24). Yesu anatulutsa chiwandacho mwa munthuyo, ndipo anthu anayankhapo kuti: "Ichi nchiyani? Chiphunzitso chatsopano! Ndi mphamvu alamula ingakhale mizimu yonyansa, ndipo imvera Iye" (v. 27).

Yesu anapereka utumiki wake wophunzitsa kwa ophunzira ake (Mateyu 28:19-20). Pakuona zomwe amachita, anaphunzira mmene angaphunzitsire ena. Monga abusa aChipentekoste, tiyenera kuchita chimodzimodzi. Tiyenera kutsanzira utumiki wa kuphunzitsa wa Yesu.

MBUSA NGATI MPHUNZITSI WAMKULU

Monga Mbusa, muyenera kudziona ngati "mphunzitsi wamkulu" mu mpingo umene mwaitanidwa kuti muutsogolere. Mwanjira ina, simuyenera kukhala mphunzitsi waluso wa Mau a Mulungu,muyenera kuphunzitsa ena mwakhama kuti azichita zomwezo. Izi n'zimene Yesu ndi atumwi ake anachita. Monga mphunzitsi wamkulu, muli ndi maudindo atatu: (1) muyenera kukulitsa utumiki wanu wophunzitsa; (2) muyenera kukulitsa luso la kuphunzitsa la ena; ndipo (3) muyenera kulinganiza utumiki wophunzitsa wa mpingo. Tiyeni tiwone chilichonse mwa maudindo awa:

Kudzitukula Wekha

Choyamba, monga mphunzitsi wamkulu mu mpingo, muyenera kuyesetsa kuwongolera utumiki wanu wophunzitsa. Paulo analembera Timoteo kuti woyang'anira, kapena kuti Mbusa, ayenera kukhala "wokhoza kuphunzitsa" (1 Tim. 3:2). Paulo analembera Timoteo kuti: Kapena, monga momwe Baibulo lina limanenera, Mbusa ayenera kukhala "waluso pophunzitsa" M'kalata yake yopita kwa Akhristu a ku Roma, Paulo ananena kuti anthu amene ali ndi mphatso ya kuphunzitsa ayenera kugwiritsa ntchito mphatso imeneyi mokhulupirika (Aroma 12:6-8). Mwa kuyankhula kwina, ayenera kuyesetsa mwakhama kukulitsa luso lawo monga mphunzitsi.Ngakhale kuti luso la kuphunzitsa lingaperekedwe monga mphatso yauzimu, liyenera kukulitsidwa monga luso lophunziridwa. Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kukhala wophunzira Mawu a Mulungu moyo wanu wonse. Ndipo muyenera kuyesetsa kukulitsa luso lanu la kuphunzitsa (2 Tim. 2:15).

Munthu wina ananena kuti kuphunzitsa n'koposa kulankhula, ndipo kuphunzira kumaposa kumvetsera. Cholinga chachikulu cha kuphunzitsa ndikubweretsa kusintha kwa moyo wa ophunzira. Motero kuphunzitsa kogwira mtima kumaphatikizapo kugwiritsira ntchito kawirikawiri choonadi chimene chikuphunzitsidwa. Pozindikira zimenezi, sitiyenera kukhutira podziwa kuti mamembala athu amangomva mawu athu. Tiyenera kukhutitsidwa pamene tiwona miyoyo yawo ikusintha. Choncho, sitiyenera kungofotokoza zimene Mawu a Mulungu akutanthauza, tiyenera kuthandiza okhulupirira kugwiritsa ntchito choonadi cha m'Malemba pa moyo wawo.

Komanso, monga abusa a Chipentekoste, tiyenera kumvetsetsa kuti nthawi zambiri timaphunzitsa ndi zochita zathu kuposa mawu athu. Paulo anamvetsa

mfundo imeneyi. Choncho anaitanira Akhristu a ku Akorinto kuti: “Khalani onditsanza ine, monga inenso nditsanza Khristu” (1 Ako. 11:1). Yesu ankagwiritsa ntchito mfundo imeneyi pamene anauza ophunzira ake kuti: “Wophunzira saposa mphunzitsi wake; koma yense, m’mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wake” (Luka 6:40). Yesu ankatsatira mfundo imeneyi. Choncho, monga zitsanzo kwa mpingo, tiyenera kugwiritsa ntchito zimene timaphunzitsa kwa ena.

Tukulani Anthu Ena

Chachiwiri, monga mphunzitsi wamkulu mu mpingo, muyenera kuyesetsa kukulitsa luso la kuphunzitsa la atsogoleri ena ampingo. Pamene mpingo ukukula kwambiri, padzakhalanso atsogoleri otsogolera mautumiki omwe akubwera. Kuti atsogolere bwino, aliyense adzafunika kukulitsa luso linalake la kuphunzitsa. Muyenera kuwonetsetsa kuti mtsogoleri aliyense watsopano akulandira maphunziro oyenera kuti atsogolere bwino.

Pochita izi, muyenera kuphunzitsa atsogoleri ena momwe angaphunzirire ndi kumasulira bwino Baibulo. Ndipo muyenerakuwasonyeza mmene angakonzekerere ndi kuphunzitsa ena Mawu a Mulungu. Ngati muchita zinthu izi, mpingo udzakhala ndi aphunzitsi aluso nthawi zonse. Ngati mulephera kuphunzitsa atsogoleri a mpingo mmene angaphunzitsire, utumiki wophunzitsa mpingo udzasokonekera ndipo kukula kwauzimu kwa Akhristu kudzavutika.

KUKONZEKERETSA MPINGO KU KUPHUNZITSA

Pomaliza, monga mphunzitsi wamkulu, muyenera kukhala woimira mpingo wa maphunziro AchiKhristu. Muyenera kukonzekeretsa mosamalitsa ndikupititsa patsogolo mwachangu mautumiki ophunzitsa mpingo. Muyeneranso kuwonetsetsa kuti mautumiki ophunzitsa mpingo akukhudza munthu aliyense wa msinkhu uliwonse mu mpingo. Maphunziro mu mpingo ayenera kukhala ndi izi:

Maphunziro a Baibulo (Sande Sukulu)

Palibe maphunziro mu mpingo omwe ali ndi kuthekera kwakukuru kuposa Maphunziro a Baibulo (Sande Sukulu). Maphunziro a Baibulo (Sande Sukulu) ndi utumiki wokhawo pampingo umene umafikira munthu aliyense wa m’sinkhu uliwonse mumsonkhano. Choncho muyenera kuyesetsa kuonetsetsa kuti mpingo umene mukutsogolera uli ndi Maphunziro a Baibulo olinganizidwa bwino ndi

opatsidwa chuma bwino choyendetsera utumiki umenewu. Muyeneranso kuonetsetsa kuti Gawo la utumiki umenewu likutsogoleredwa ndi munthu woyenerera. Chifukwa chakuti utumiki umenewu ndi wofunika kwambiri, muyenera kukhala ochitachitachita m'sukuluyi. Ndipo muyenera kuyang'anira ntchito zake nthawi zonse ndikuyesetsa kukonza bwino.[1]

Milaga

Ngati zingachitike moyenera, milaga ndi njira ina yabwino yophunzitsira ophunzira. Magulu amenewa amakumana mlungu ndi mlungu m'nyumba za anthu osankhidwa ampingo kaamba kachiyanjano, mapemphero, ndi phunziro la Baibulo. Monga mphunzitsi wamkulu, muyenera kuwonetsetsa kuti gulu lililonse lapanyumba likutsogozedwa ndi mtsogoleri wokhulupirika, wophunzitsidwa bwino. Nthawi iyenera kuperekedwa mumsonkhano uliwonse wamagulu kuti akambirane momasuka pa mutu wosankhidwa wa m'Baibulo. Inu, kapena wina amene mwamupatsa ntchito, muyenera kuyang'anitsitsa zomwe zikuphunzitsidwa mu gulu lililonse. Ndinu omasuka kupereka ndondomeko ya kaphunzitsidwe ka m'magulu.[2]

Utumiki wa Mzigawo

Utumiki wa mzigawo mu mpingo uyenera kuwonedwa ngati njira yophunzitsira ophunzira. Zigawozi ndi monga Utumiki wa Abambo, Utumiki wa Amayi, Utumiki wa Achinyamata, Utumiki wa Ana, ndi ena. Maphunziro a m'Baibulo othandiza ayenera kuphunzitsidwa nthawi iliyonse pamene limodzi la magulu amenewa likumana.

Sukulu Ya Utumiki

Mbusa aliyense wa Chipentekoste aganizire zoyambitsa Sukulu ya Utumiki mu mpingo wake. Sukulu ya Utumiki ndi sukulu imene cholinga chake ndi "kukonzekeretsa oyera mtima ku ntchito za utumiki" (Aefeso. 4:12). Cholinga

[1] Buku la Chiyembezo cha Afirika Kukhala Choonadi (Africa's Hope Living the Truth) ndi maphunziro a achikulire a Sukulu ya Baibulo (Sande Sukulu) amene amatengera ophunzira Baibulo lonse m'zaka zisanu ndi ziwiri. Apezeni mwaulere pa https://africaatts.org/resources/.

[2] Mndandanda wa Chiyembekozo cha Afirika Mizu ya Chikhulupiriro ndi maphunziro apamwamba omwe akupezeka mwaulere pa https://africaatts.org/resources/.

chake ndi kuphunzitsa ogwira ntchito za utumiki mu mpingo. M'sukuluyi, abusa amaphunzitsa maphunziro okhudza zinthu zothandiza monga kulalikira,kuphunzitsa, kupemphera, kuwombola miyoyo, kudzala mipingo, luso la utsogoleri, ndi zina. Maphunziro oterowo adzathandiza kuti mpingo ukhale ndi antchito oyenerera okhazikika.

Pamene mpingo ukukula ndi kuchita bwino, mungafunikekupereka gawo la maphunziro anu kwa ena. Komabe, monga mphunzitsi wamkulu wa mpingo, muyenera kukhala otanganidwa nthawi zonse mu utumiki wa kuphunzitsa mpingo ndi kuphunzitsa mautumiki.

Yesu anafunsa Petro katatu kuti, "Simoni mwana wa Yona, kodi undikonda Ine? Ndipo Petro anayankha katatu, "Inde, Ambuye, mudziwa kuti ndikukondani Inu." Nthawi zonse Yesu anamuuza kuti, "Dyetsa anaankhosa anga," kapena "Weta nkhosa zanga" (Yoh. 21:15-18). Ngati Petro ankakondadi Yesu, akanachita zimene Mbuye wake anamulamula n'kudyetsa nkhosa za Mulungu mokhulupirika.

Lero lino, Yesu akufunsa abusa a Chipentekoste ku Afirika yense funso lomwelo: "Kodi undikonda Ine? Ndipo akupereka lamulo lomwelo kwa iwo lomwe adapereka kwa Petro: "Dyetsa nkhosa zanga." Monga umboni wa chikondi chawo, Yesu akulamula abusa amenewa kuona mozama ntchito yawo yopatsidwa ndi Mulungu ya kusamalira anthu a Mulungu mwa kuwaphunzitsa Mawu a Mulungu mokhulupirika.

~ Mutu 18 ~

Kutsogolera Mpingo M’kulambira

Mdziko lina la ku Chigawo cha Pakati ku Afirika, mnyamata wina wophunzira ntchito anapatsidwa ntchito yotumikira pansi pa Mbusa wokalamba. Mbusayo anapempha wophunzirayo kuti atsogolere mpingo polambira Lamlungu lotsatira m’mawa. Komabe, mnyamatayo sanasangalale. Ankalakalaka abusa akalewo atamupempha kuti azilalikira. Iye ankaona kuti kutsogolera chipembedzo kunali kumuchotsera ulemu wake monga Mbusa.Komanso, chifukwa chakuti anadzazidwa ndi Mzimu ali ku sukulu ya Baibulo, iye sanaone chifukwa chopempherera kapena kukonzekera chochitikacho.

Monga momwe tingayembekezere, pansi pa utsogoleri wake lamulungu m’mawa, utumiki wa kulambira sunakayende bwino. Pakadapanda kulowerera mwaluso kwa Mbusa wakaleyo, utumikiwo ukanakhala watsoka. Kuyambira nthawi imeneyo, Mbusayo wakhala akusankha atsogoleri ake achipembedzo mosamala kwambiri. Tsopano amalola anthu okhwima maganizo okha, ophunzitsidwa bwino kutumikira monga atsogoleri a kulambira.

CHOFUNIKIRA CHA KULAMBIRA KOONA

M’Baibulo, mawu achihebri ndi achigiriki otanthauza kulambira amatanthauza kugwada ndi kupereka ulemu kwa Mulungu. Amapereka lingaliro la kusonyeza chiyamikiro modzichepetsa kwa Iye, ndi kumkweza Iye kaamba ka

chiyero Chake, ulemerero, ndi mphamvu (Yesaya. 6:1-3; Chivumbulutso. 7:11-12).

Lambirani mu Mzimu ndi Choonadi

Yesu anabweretsa poyera tanthauzo la kulambira koona pamene anauza mkazi wa Kusamariya kuti: "Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano ilipo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'choonadi; pakuti Mulungu ndiye mzimu, ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'choonadi" (Yohane 4:23-24). M'ndime imeneyi, Yesu anavumbula mfundo zinayi zofunika kwambiri zokhudza kulambila koona:

1. Mulungu ndi mzimu. Pokhala mzimu Mulungu, Iye alibe malire ndi nthawi kapena malo. Choncho akhoza kulambiridwa nthawi ina iliyonse komanso pamalo aliwonse.

2. Mulungu akufunafuna olambira woona. Iye akufunafuna anthu amene adzamulambire kuchokera pansi pa mitima yawo osati ndi maonekedwe akunja ndi miyambo (onani Marko 12:33).

3. Kupembedza koona kuyenera kuchitidwa mu Mzimu ndi mchoonadi. Popeza Mulungu ndi mzimu, amene amamulambira ayenera kumulambira mumzimu. Popeza Iye ndi choonadi chenicheni, ayenera kumupembedza mogwirizana ndi choonadi chimene chavumbulutsidwa m'Malemba.

4. Ino ndiyo nthawi. Nthawi yolambira Mulungu mu Mzimu ndi m'choonadi ndi ino.

Kulambira ndiko ntchito yopatulika ya kuyankha moyenerera kukhalapo kwa Mulungu, monga anachitira akulu makumi awiri mphambu zinayi a mu Chivumbulutso mutu 4. Pochita mantha ndi kupezeka kwa Khristu, "amagwa pamaso pa Iye wakukhala pa mpando wachifumu, namlambira" (v.10). Pamene anthu a Mulungu amamulambira, Iye amaonetsera kupezeka Kwake pakati pawo, kuwatakasa iwo kumulambira mochuluka.

Zoyembekeza za Chipentekoste

Monga Mbusa wa Chipentekoste, ndikofunikira kuti mumvetsetse chikhalidwe chapadera cha kulambira kwa Chipentekoste. Kulambira kwa

Chipentekoste ndikwapadera chifukwa kumatsindika kukumana ndi Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera. Motero iwo a Chipentekoste amafika mu kulambira ndi ziyembekezo zosiyana ndi zimene ambiri omwe si a Chipentekoste amakhala nazo. Anthu ambiri omwe si a Chipentekoste amafika m'kulambira ndi cholinga chofuna kukwaniritsa udindo wawo wachipembedzo kapena kuchita miyambo yachipembedzo. Komabe, wa Chipentekoste woona amafika m'kulambira ndi cholinga china. Cholinga chake ndi kukumana ndi Khristu wamoyo, ndipo chifukwa cha kukumana kumeneko, kusandulika ndi Mzimu Wake (2 Ako. 3:17-18).

Kusintha uku kungakhale kochepa kapena kwakukulu, kobisika kapena kochititsa chidwi. Kusandulika kwamachawi kungakhale kuti, pamene wokhulupirira akumana ndi Khristu mu kulambira, amapeza mphamvu zatsopano ndi chisangalalo pakumtumikira Iye. Kusintha kochititsa chidwi kwambiri kungakhale kuti wolambirayo akumana ndi Khristu woukitsidwayo ndipo amachiritsidwa mozizwitsa kapena kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.

Kusandulika kotereku kumadza m'njira ziwiri: mwa Mzimu ndi mwa choonadi (Yoh. 4:23). Pamene olambira akuyandikira kwa Mulungu, Iye amawonetsera kupezeka Kwake. Pamene akukumana ndi kuyankha mwachikhulupiriro ku kupezeka kwa Mulungu (kupembedza mu Mzimu) amasandulika kukhala chifaniziro cha Khristu (2 Ako. 3:17-18). Ndiponso, pamene amayankhapo mwachikhulupiriro ku Mawu olalikidwa (kulambira m'chowonadi), amakhala akunka namasandulikabe.

KUKONZEKERETSA MPINGO KU KULAMBIRA

Monga Mbusa, ndi udindo wanu kukonzekeretsa mpingo kuti ulambire Mulungu mowona. Muyenerakuwonetsetsa kuti anthu akudziwa momwe angamupembedzere mu Mzimu ndi mchoonadi. Muyenera kutsimikiziranso kuti anthu amatsatiradi kulambira koteroko. Mutha kuchita izi m'njira zitatu:

Mwa kuphunzitsa za Kulambira

Choyamba, mungaphunzitse mpingo chimene Baibulo limanena pa nkhani ya kulambira. Mutha kuchita izi kudzera mu ulaliki, chilimbikitso, ndi mindandanda ya maphunziro. Njira imodzi yabwino imene Mbusa wa Chipentekoste angaphunzitse anthu ake mmene angalambirire Mulungu mu Mzimu ndi m'choonadi ndi kuwaonetsera. Anthuwo ayenera kuona Mbusa wawo akulambira

Mulungu ndi mtima wonse. Mbusa wina wokhwima mwauzimu analangiza iwo omwe amachita maphunziro a ubusa kuti: "Ngati mudzalambira Mulungu mowona mtima, anthu anu adzakutsatirani, ndipo nawonso adzamulambira."

Komanso, muyenera kusonyeza anthu mmene angalambirire Mulungu ndi moyo wawo. Mungathe kuchita izi pakukhala moyo wachiyero ndi kukhala njira ya madalitso a Mzimu kwa ena.

Mwa Kuyang'anira Ntchito Zakulambira

Chachiwiri, paudindo wanu ngati woyang'anira, muyenera kuyang'anira mwapemphero misonkhano yachipembedzo kuti muwonetsetse kuti anthu akutsogozedwa pakulambira Mulungu mu Mzimu ndi m'choonadi. Muyenera kuti zonse mu utumiki wa mpingo zichitike "moyenera ndi mwadongosolo" (1 Ako. 14:40). M'mawu ena, muyenera kuonetsetsa kuti kupembedza kukuchitika m'njira imene imalemekezadi Mulungu ndi kuyandikitsa anthu kuyandikira kwa Khristu (1 Ako. 10:31).

Mwa kuphunzitsa Gulu la Matamando (Olambira)

Njira yachitatu imene mungatsimikizire kuti mpingo umalambira Mulungu mu Mzimu ndi m'choonadi ndi kuphunzitsa mwachikondi gulu la Matamando la mpingo. Muyenera kuwaphunzitsa kuti udindo wawo ndi kutsogolera mpingo ku matamando ndi kulambira motsogozedwa ndi Mzimu. Chotero muyenera kukhala nawo nthawi, kuwaphunzitsa mmene angalambire Mulungu moonadi, ndi kuwasonyeza mmene angatsogolere ena m'kulambira koona**.**

Kuphatikiza apo, muyenera kupemphera pafupipafupi ndi mamembala a gulu limeneli, kuwonetsetsa kuti adzazidwa ndi Mzimu Woyera komanso kuti akudziwa kutsatira chitsogozo cha Mzimu. Muyeneranso kuwonetsetsa kuti gululi likusankha nyimbo zauzimu komanso za m'malemba. Monga Mbusa, muyenera kusungitsa ufulu kuvomereza nyimbo zonse zatsopano zisanagwiritsidwe ntchitopachipembedzo chilichonse.

Komanso, monga Mbusa wa mpingo muyenera kukumbukira kuti, ndinu mtsogoleri wachiwiri wamkulu wachipembedzo pambuyo pa Mzimu. Izi sizikutanthauza kuti mudzaima pamaso pa mpingo kutsogolera anthu kutamanda ndi kulambira. Zikutanthauza kuti muyenera kukhala woyang'anira ntchitoyo nthawi zonse. Gulu la Matamando liyenera kumvetsetsa kuti, monga Mbusa,

mutha kuima ndikuyang'anira ntchito nthawi iliyonse. Izi zikachitika, gulu la Matamando liyenera kusiya ntchitoyo m'manja mwanu nthawi yomweyo.

Pamene kulambira kowona mu Mzimu ndi m'choonadikukuchitika, madalitso amphamvu amabwera ku mpingo: Mulungu amalemekezedwa, kupezeka kwa Mzimu kumaonekera, ndipo thupi la Khristu limalimbikitsidwa.

KUTSOGOLERA MPINGO KU KULAMBIRA

Mbusa wa Chipentekoste amene amamvetsa choonadi ichi adzakhala ndi chidwi chotsogolera mpingo wake ku kulambira kotsogozedwa ndi Mzimu. Izi zikutanthauza kuti, mu nthawi ya kupembedza, muyenera kukhala omvetsera ku mawu a Mzimu, ndipo muyenera kufulumira kutsatira zomwe Iye akufuna. Monga Mose m'chipululu, muyenera kukhala okonzeka kutsogolera mpingo kuyenda pamene mtambo ukuyenda, ndi kuima pamene mtambo uima (fanizilani Eksodo 40:34-38).

Kulimbikitsa Kutengapo Mbali

Monga mtsogoleri wauzimu wa mpingo, muyenera kulimbikitsa aliyense amene akupezekapo kuti atenge nawo mbali pa kulambira. Alimbikitseni kusonyeza matamando awo kwa Mulungu mwa kukweza manja awo, kuimba, kufuula, kuchitira umboni, kuwomba m'manja, kuvina, kugwada, kapena mawu ena aliwonse a m'Malemba osonyeza kulambira. Muyenera kuwaphunzitsanso anthu kuti akupembedza Mulungu pamene akupereka chachikhumi ndi zopereka zawo. Pochita izi, amalemekeza Mulungu ndi chuma chawo ndi zipatso zoyamba za zokolola zawo (Miy. 3:9).

Pokhazikitsa Magulu Oimba (Makwaya)

Kuonjezera apo, Mbusa wa Chipentekoste alimbikitse chitukuko cha makwaya ndi magulu ena anyimbo kuti azitumikira m'mapemphero a mpingo ndi kufalitsa uthenga wabwino. Gulu lililonse kapena kwaya nthawi zonse ikhale yovomerezeka kwa abusa kapena mtsogoleri wa maimbidwe. Choncho muyenera kugwira ntchito ndi magulu oimba mofanana ndi mmene mumagwirira ntchito ndi gulu la matamando, kuwaphunzitsa kusiyana pakati pa kusangalatsa anthu ndi utumiki woona mu Mzimu.

Kusamalira Mphatso Zauzimu

Monga mtsogoleri wauzimu wa mpingo, mbusa wa Chipentekoste akuyeneranso kulimbikitsa kugwiritsa ntchito mphatso za uzimu pa mapemphero. Izi zinali zodziwika mu mpingo wa Chipangano Chatsopano, ndipo ziyenera kukhala zodziwika bwino m'mapemphero amasiku ano (onani Machitidwe 11:27-28; 13:2).

Paulo analimbikitsa mpingo wa ku Akorinto "funitsitsani mphatso zauzimu" (1 Ako. 14:1). Iye anawalangizanso kuti: "Pamene musonkhana, yense ali nalo salimo, ali nacho chiphunzitso, ali nalo vumbulutso, ali nalo lilime, ali nacho chimasuliro" (1 Ako. 14:26). Choncho, ngati Mbusa, muyenera kuphunzitsa mpingo za mphatso za uzimu. Ndipo mulore kuti mphatsozi zipeze malo mu mautumiki a mpingo. Pa nthawi yomweyo, muyenera kusamala kuti musagwiritse ntchito molakwika mphatso za uzimu (1 Ako. 14:26-33).[1]

Udindo wa Nyimbo

Nyimbo ndi kuimba zimagwira ntchito yofunikira kwambiri pa kulambira. Wamasalimo akulimbikitsa anthu a Mulungu kuti: "Fuulani mokondwera mwa Yehova, Inu olungama mtima, oongoka mtima ayenera kulemekeza. Yamikani Yehova ndi zeze; muimbireni ndi chisakasa cha zingwe khumi. Mumuimbire Iye nyimbo yatsopano; muimbe mwaluso kumveketsa mau" (Masalimo 33:1-

Malinga ndi kunena kwa Paulo, nyimbo ndi kuyimba zimagwira ntchito zosachepera zinayi polambira: kulemekeza Mulungu, kusonyeza chiyamiko kwa Iye, kuphunzitsa choonadi cha m'Malemba, ndi kulangiza okhulupirira kukhala ndi moyo kwa Iye. Mtumwiyo anatsindika zinthu ziwiri zoyambirira m'kalata yake yopita ku mpingo wa Aefeso: "Ndi kudzilankhulira nokha ndimasalimo, ndi mayamiko, ndi nyimbo zauzimu, kuimbira ndi kuimba m'malimba Ambuye mumtima mwanu, ndi kuyamika Mulungu Atate masiku onse" (Aefeso. 5:19-20). Iye anatsindikanso zinthu ziwiri m'kalata yake yopita kwa Akolose kuti: "Phunzitsani ndi kulangizana wina ndi mnzake ndi nzeru zonse, mwa masalmo, ndi nyimbo, ndi nyimbo za mzimu" (Akolose. 3:16).

[1] Onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

Chenjezo Lapanthawi Yake

Chenjezo la panthawi yake liyenera kuperekedwa pano. Nthawi zambiri anthu amakopeka ndi mipingo ya Chipentekoste chifukwa cha kuimba kwawo mwachidwi. Izi ndi zabwino, ndipo muyenera kulimbikitsa mchitidwewu. Koma nthawi yomweyo, musalole kuti mpingo upereke "moto wachilendo" kwa Yehova (Lev. 10:1). Mwa kuyankhula kwina, muyenera kuwonetsetsa kuti kuyimba ndi kuvina kusakhale chionetsero cha thupi koma kuyankha kwa mitima yoyeretsedwa ku Mzimu wa Mulungu. Chotero, monga Mbusa, simuyenera kulola kuti nyimbozo zikhale zaphokoso kuti mpaka zilepheretse kulambira kowona kochokera pansi pamtima.Kumbukirani uphungu wa Paulo wakuti: "thupi lililonse lisadzitamande pamaso pa Mulungu" (1 Ako. 1:29). Mulungu asadzafike pakunena mpingo wanu kuti, "Mundichotsere phokoso la nyimbo zanu; sindifuna kumva mayimbidwe a zisakasa zanu" (Amosi 5:23)

MAVUTO AWIRI AKULAMBIRA

Afirika ndi dziko lalikulu lokhala ndi mitundu ya anthu yoposa 3,000 yolankhula zinenero zoposa 2,100. Chotero sikuli kwachilendo kwa mpingo wa Chipentekoste mu Afirika kuphatikiza anthu a mafuko osiyanasiyana. Kuwonjezera pamenepo, mpingo uliwonse uli ndi magulu a zaka zosiyanasiyana. Kusiyanasiyana kumenekukumabweretsa zokonda zosiyanasiyana mu nyimbo ndi m'machitidwe opembedza. Ngati sizisamalidwa mwanzeru, zikhoza kuyambitsa kusagwirizana mu mpingo. M'malo molimbikitsa umodzi m'mpingo, misonkhano yampemphero mu mpingo ikhoza kukhala magwero a magawano.

Mavuto awiri obwera chifukwa cha kusiyana kumeneku ndi kusagwirizana pa kachitidwe ka kupembedza komanso vuto logwiritsa ntchito zilankhulo zingapo popemphera. Monga Mbusa, muyenera kuchita mwanzeru ndi zovuta zonsezi.

Nyimbo ndi Kupembedza kwake

Mipingo yambiri ya Chipentekoste ku Afirika imapeza kuti mamembala amasemphana maganizo pankhani ya nyimbo ndi kapembedzedwe. Mwachitsanzo, achichepere mu mpingo angakonde kachitidwe ka kulambira kofuula, kokangalika, pamene okalamba amasankha machitidwe abata, odzisunga. Wina amakonda nyimbo zamasiku ano pomwe wina amakonda nyimbo zachikhalidwe. Monga Mbusa, muyenera kugwiritsa ntchito nzeru zakuya pothana

ndi nkhaniyi. Ndipo muyenera kusiyanitsa pakati pa kalambilidwe ndi zinthu mu kulambira.

Maonekedwe amalankhula za zokonda za munthu payekhapayekha kupembedza kwakunja; chinthu chimalankhula za zenizeni zake zamkati. Kupembedza ndi kukweza Mulungu ndi mtima wonse (onani Marko 7:6-7). Zoona zake n'zakuti Mkhristu akhoza kulambira Mulungu mowona mtima pogwiritsa ntchito machitidwe osiyanasiyana. Kaya munthu agwiritse ntchito kachitidwe kanji, ngati achita izi mu Mzimu ndi mchoonadi, Mulungu amavomereza. Ngati sichichitidwa mu Mzimu ndi m'chowonadi, icho chimakanidwa. Chotero muyenera kuphunzitsa anthu kulemekeza zokonda za wina ndi mnzake m'kulambira. Muyenera kuti "tilondole zinthu za mtendere, ndi zinthuzakulimbikitsana wina ndi mnzake" (Aroma 14:19).

Mbusa wanzeru adzaphunzitsa okalamba kuti azisangalala akamaona achinyamata akulambira Mulungu m'njira yotsegula mitima yawo kwa Mulungu ndi kumayandikira kwa iye. Chifukwa chokonda achichepere, iwo ayenera kukhala ofunitsitsa kugwirizana nawo m'kulambira kwawo kwa Mulungu. Mofananamo, muyenera kuphunzitsa achichepere kulemekeza zosowa ndi zokonda za akulu awo, ndi kugwirizana nawo ndi mtima wonse m'kulambira kwawo. Mudzafunanso kuphunzitsa achinyamata kukonda ndi kuyamikira nyimbo zamphamvu za chitsitsimutso za chikhulupiriro.

Mbusa wanzeru wa Chipentekoste adzaonetsetsa kuti mapemphero a mpingo akhale ndi nyimbo zatsopano ndi zakale,zamakono ndi zachikhalidwe. Adzakumbukira kuti chofunika n'chakuti wokhulupirira aliyense akumane ndi Mzimu wa Mulungu polambira ndi kuti asonyeze mowona mtima kudzipereka kwawo kwa Khristu.

Zinenero Zambiri

Monga tanenera kale, mipingo yambiri ya Chipentekoste kuAfirika kuno kumapezeka anthu olankhula zinenero zosiyanasiyana. Nkhani iyi imabweretsa zovuta zina kwa abusa a Chipentekoste. Ngati mpingo wasankha kuchita mapemphero ake m'chinenero chodziwika bwino cha m'deralo-kunyalanyaza ena onse—umakhala pachiwopsezo chochotsa anthu a zilankhulo zina. Komabe, ngati, umagwiritsa ntchito zilankhulo zingapo pakupembedza, mpingo umakhala pachiwopsezo choyambitsa kusakhutira pakati pa okhulupirira amderalo. Choncho muyenera kusamalira izi mwanzeru. Muyenera kuwonetsetsa kuti

mapemphero a mpingo amakopa chikhalidwe chomwe chilipo, pomwe nthawi yomweyo, kulandira ena. Mudzafunika kufunafuna nzeru za Mulungu pothana ndi nkhaniyi. Inu ndi gulu lanu la utsogoleri mufunika kupemphera kuti mukonze zinthu monga izi:

- Kodi chinenero chachikulu chimene mpingo udzagwiritsa ntchito polambira ndi chiti?
- Ndi zilankhulo zina ziti zomwe zidzagwiritsidwe ntchito? Kodi zilankhulo zimenezi zidzagwiritsidwa ntchito liti ndipo m'njira zake ziti?
- Kodi zolengeza, mapemphero apagulu, ndi ulaliki zidzamasuliridwa m'chinenero chiti?
- Ndi zinenero ziti zimene zidzagwiritsidwe ntchito poimba? Kodi zinenerozi zidzagwiritsidwa ntchito liti ndipo zidzagwiritsidwa ntchito bwanji?
- Kodi ndi magulu ati a zilankhulo mumpingo amene akunyalanyazidwa? Kodi tingawathandize bwanji kuti adzimva kuti ali nawo limodzi?

Pamene kuli kwakuti mpingo uliwonse udzafunikira kupeza njira yakeyake yochitira ndi nkhani imeneyi, mfundo zina zazikulu zimagwira ntchito. Mwachitsanzo, pokonzekera kupembedza, muyenera kuonetsetsa kuti aliyense amene abwera ku msonkhano akumva kulandiridwa komanso kuphatikizidwa. Cholinga china n'chakuti onse amene apezekapo azilimbikitsidwa. Kuonjezera apo, mapemphero ayenera kukhala ogwirizanitsa osati kugawanitsa mpingo. Kutsatira mfundo zimenezi kudzathandiza kuonetsetsa kuti ziganizo zabwino zatsatiridwa.

Mipingo ina ya m'tauni, monga mipingo yamaiko onse, idzafuna kuchita misonkhano yawo m'chinenero chofala cha ku Ulaya cha dzikolo. Mipingo ina idzafuna kugwiritsa ntchito chilankhulo cha ku Afirika. Ena adzafuna kumasulira ntchito yonse. Ena adzamasulira ulaliki wokha. Enanso angafune kupita kuzinthu zingapo ndipo msonkhano uliwonse ukuchitidwa m'zilankhulo zosiyanasiyana. Mulimonse momwe mpingo wanu ungatsatire, cholinga chanu chikhale kuwonetsetsa kuti aliyense amene amabwera ku mapemphero akumva kuti akulemekezedwa ndi kuphatikizidwa.

Udindo waukulu wa Mbusa aliyense wa Chipentekoste ndi kutsogolera mpingo wake ku chipembedzo choona, chodzozedwa ndi Mzimu. Angachite izi

pophunzitsa anthu tanthauzo la kulambira Mulungu mu Mzimu ndi m'choonadi, ndiponso potengera chitsanzo cha moyo wake weniweni wa kulambira.

~ Mutu 19 ~

Kutsogolera Mpingo ku Chitsitsimutso cha Chipentekoste

Wina anafotokoza za kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera pa Tsiku la Pentekoste ngati chitsitsimutso choyamba cha Mpingo. Patsiku limenelo, Mulungu anatsanulira Mzimu Wake koyamba pa Mpingo, kuudzaza ndi moyo ndi kuupatsa mphamvu kuti ukwaniritse ntchito yake padziko lapansi. Gulu la masiku ano la Chipentekoste limachokera ku zomwe zinachitika pa tsikulo.

Kukhala wa Chipentekoste kumatanthauza kuti munthu amavomereza zochitika ndi cholinga cha Pentekoste. Zochitika pa Pentekoste ndizochitika zauzimu zamphamvu zomwe Baibulo limalongosola ngati ubatizo, kapena kumizidwa mu Mzimu Woyera (Luka 3:16; Mach. 1:5). Cholinga cha Pentekoste ndi kupatsa mphamvu yakuchitira umboni kuyambira mnyumba yakwanu ndi kumalekezero a dziko lapansi (Mach. 1:8).

Mosiyana ndi mipingo yosakhala ya Chipentekoste, mpingo wa Chipentekoste sungakhale wowona ku cholinga chake ndi kuyitana popanda kutsanulidwa mobwerezabwereza kwa Mzimu Woyera. Monga momwe thupi lidzafa ngati litasiya kupuma mpweya, mpingo wa Chipentekoste udzafa ngati usiya kupuma mu Mzimu wa Mulungu. Mwa kuyankhula kwina, kuti ukhale wa Chipentekoste weniweni mpingo uyenera kukhala ndi chitsitsimutso cha Pentekoste. Yesu anafotokoza kuti: “Wopatsa moyo ndi mzimu; thupi silithandiza

konse" (Yoh. 6:63). Mutu uwu ukambirana momwe inu ngati Mbusa wa Chipentekoste mungatsogolere mpingo wanu ku chitsitsimutso chotere.

KUMVETSA ZA CHITSITSIMUTSO

Mbusa wa Chipentekoste asanatsogolere mpingo wake ku chitsitsimutso, ayenera kukhala ndi chithunzithunzi m'maganizo mwake momwe chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano chimawonekera. Komabe, mwatsoka, abusa ambiri a Chipentekoste ali ndi malingaliro opotoka a chitsitsimutso. Iwo atenga lingaliro lawo la chitsitsimutso, osati kuchokera mu lemba, koma kuchokera ku chikhalidwe chotchuka cha mpingo. Chifukwa cha zimenezi, amaona chitsitsimutso monga mpingo wodzazidwa ndi anthu akuimba mosangalala, kuvina, ndi kutamanda Mulungu. Kapena amaganiza za chitsitsimutso ngati Mulungu akutsanulira madalitso akuthupi ndi chitukuko pa anthu Ake. Ngakhale kuti zina mwa zinthu zimenezi zikhoza kutsagana ndi chitsitsimutso, sizifotokoza za chitsitsimutso choona monga momwe chikusonyezedwera m'buku la Machitidwe.

Ngakhale kuti mawu akuti *chitsitsimutso* sapezeka muChipangano Chatsopano, lingaliro la kukonzanso kwa uzimu ndilo (onani Machitidwe 3:19). Chitsitsimutso chimanena za moyo watsopano ndipo chimatanthauza kubwezeretsedwa kwa chidziwitso, machitachita, ndi mphamvu. Icho chimene mu Chipangano Chakale chimatchedwa kuti chitsitsimutso (Masalimo 85:6; Hab. 3:2), mu Chipangano Chatsopano chimafotokozeredwa kuti ndi kutsanulidwa kwa Mzimu (Mach. 2:17-18). M'mitu iwiri yoyambirira ya Machitidwe, Baibulo limatchula zinthu zitatu zofunika pa chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano:

- Choyamba, anthu a Mulungu amabatizidwa, ndipo motero amapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera (Mach. 1:8; 2:1-4).
- Kenako, anthu a Mulungu amayamba kulengeza molimba mtima za Khristu kwa otayika mu mphamvu ya Mzimu Woyera (Mach. 2:14-40; 4:31).
- Pomaliza, anthu otayika alapa, naika chikhulupiriro chawo mwa Khristu, ndipo amapulumutsidwa (Mach. 2:41, 47; 5:12-16).

Zotsatira zina za kutsanulidwa kwenikweni kwa Mzimu Woyera monga momwe zalongosoledwera mu buku la Machitidwe ndi machiritso, zizindikiro, ndi zodabwitsa (Mach. 2:43; 5:12-16). Zozizwitsa zauzimu zimenezi kawirikawiri zimadzetsa chisangalalo chachikulu, misonkhano yampingo yosangalatsa, ndi kukula kwampingo. Komabe, zinthu zitatu zofunika zatsala pamtima pa

chitsitsimutso chenicheni cha Chipentekoste: kulimbikitsidwa mu uzimu, umboni wamphamvu, ndi anthu kubwera kwa Khristu. Ngati chimodzi mwa zinthu zitatu izi chikusowa, chitsitsimutso chenicheni cha Chipentekoste sichinachitike.

ZITSANZO ZA M'BAIBULO

Tiyeni tifutukule pang'ono tanthauzo lathu la chitsitsimutsopoyang'anitsitsa zomwe zinachitika pa Tsiku la Pentekoste. Kuyang'ana mosamalitsa kwa Machitidwe 2 kumationetsera mfundo zisanu ndi ziwiri za chitsitsimutso chenicheni cha Chipangano Chatsopano:

Anthu Amafunafuna Mulungu

Chinthu choyamba chofunika kwambiri pa chitsitsimutso chenicheni cha Chipangano Chatsopano ndi chakuti anthu a Mulungu amafuna nkhope yake m'pemphero. Baibulo limatiuza kuti, asanatsanulidwe mzimu woyera pa Pentekoste, ophunzira 120 "anakhala chikhalire mu Kachisi, nalikuyamika Mulungu" (Luka 24:53) Choncho, Akhristu okwana 120 ankakhala m'kachisi. Limanenanso kuti "onse analikukangalika m'kupemphera, pamodzi" (Mach. 1:14). Buku la Machitidwe limagwirizanitsa pemphero ndi kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera. Tanthauzo lake ndi lodziwikiratu: Ngati mpingo ukufuna kutsitsimutsidwa kwa Chipentekoste, mamembala ayenera kufunafuna Mulungu ndi mtima wonse m'pemphero.

Mulungu Amatsanulira Mzimu Wake

Mbali yachiwiri ya chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano ndi kutsanulidwa kwa Mzimu wa Mulungu. Pa Pentekoste, poyankha mapemphero a anthu ake, Mulungu mwachisomo anatsanulira Mzimu Wake pa Mpingo. Zinachitika motere:

"Ndipo pakufika tsiku la Pentekoste, anali onse pamodzi pamalo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ochokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene analikukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekhawayekha. Ndipo anadzadzidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa." (Machitidwe 2:1-4).

Okhulupirira Amalandira Mzimu

Chinthu chachitatu cha chitsitsimutso cha M'Chipangano Chatsopano ndi chakuti okhulupirira amadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndi chinthu chimodzi kuti Mulungu atsanulire Mzimu Wake; ndi chinthu chinanso kuti anthu ake alandire Mzimu. Pa Tsiku la Pentekoste, Mzimu Woyera sanangobwera pa aliyense wa iwo, "anadzadzidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa" (Machitidwe 2:4). Motero ophunzira anabatizidwa ndi Mzimu Woyera monga momwe Yesu analonjezera (Machitidwe 1:4-5). Panthawiyo, adalandira mphamvu yakukhala mboni za Khristu kunyumba ndi kumalekezero a dziko lapansi (Machitidwe 1: 8). Anthu a Mulungu akalandira Mzimu ndi chizindikiro cha chiyambi cha chitsitsimutso chenicheni cha Chipentekoste.

Akunja Amazindikira

Gawo lachinayi la chitsitsimutso mu Chipangano Chatsopano ndi lakuti anthu akunja amazindikira zimene Mulungu akuchita pakati pa anthu ake. Pa Pentekoste, awo amene anaona kubwera kwa Mzimu kwa ophunzira ndi kumvetsera pamene anali kulankhula m'zinenero zomwe sanaziphunzire 'anadabwa onse, nathedwa nzeru, nanena wina ndi mnzake, Kodi ichi nchiyani?" (Mach. 2:12).

Uthenga Wabwino Ukulalikidwa

Mbali yachisanu ya chitsitsimutso chenicheni cha Chipangano Chatsopano ndi kulalikira uthenga wabwino molimba mtima, zmouziridwa ndi Mzimu. Izi n'zimene zinachitika pa Pentekoste. Petro atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, anayimirira ndi kulalikira uthenga wabwino molimba mtima kwa khamu la anthu lomwelinasonkhana. Anawauza za Yesu ndikuwaitanira ku kulapa ndi chikhulupiriro (Mach. 2:14-40). Onse amene anadzazidwa ndi Mzimu anagwirizana ndi Petro kuchitira umboni za Khristu (v. 47).

Ambiri Apulumutsidwa

Chinthu chachisanu ndi chimodzi cha chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano ndichoti ambiri amalabadira uthenga wabwino ndikupulumutsidwa. Pa Pentekoste, chifukwa cha kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera ndi kulalikira kwa Petro wodzozedwa wa uthenga wabwino, ambiri analapa nadza kwa Ambuye. Baibulo limanena kuti omverawo 'analaswa mtima' ndipo anafunsa Petulo kuti:

“Tidzachita chiyani? Petro anayankha kuti: “Lapani, batizidwani yense wa inu m’dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera” (Machitidwe 2:37-38). Chotsatira chake, anthu 3,000 anapulumutsidwa, kubatizidwa m’madzi, ndi kuwonjezeredwa ku mpingo (v. 41). M’masiku otsatira, “Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe” (v. 47).

Mpingo Umakula

Chinthu chachisanu ndi chiwiri cha chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano ndicho kukula kwa mpingo. Pambuyo pa Pentekoste ndi kutsanulidwa kwina kwa Mzimu m'buku lonse la Machitidwe, mpingo unapitirizabe kukula ndikukula m'madera (onani Machitidwe 2:47; 4:31-3).

Mwachidule, chitsitsimutso chenicheni cha Chipentekoste chimachitika pamene anthu amakhulupirira uthenga wonena za Yesu, kudzazidwa ndi Mzimu, kenako ndi kupita kukalalikira uthenga wabwino kwa ena. Amene amalandira Uthenga Wabwinoamapulumutsidwa ndikudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Iwo eni kenaka amakhala alaliki okhulupirika a uthenga wabwino. Pamene ndondomekoyi ikubwerezedwa mobwerezabwereza, chitsitsimutso chimafalikira kutali.

UDINDO WA MBUSA

Monga Mbusa wa Chipentekoste, ndinu fungulo la chitsitsimutso mu mpingo wanu. Mutha kukhala njira yomwe imalola kuyenda kwa Mzimu kapena dziwe lomwe limatsekereza kuyenda kwake.Chilichonse chimene mukuchita-kapena kulephera kuchita—chingathe kuonetsa ngati mpingo wanu ukuona kuyenda kowona kwa Mzimu. Kuonjezera apo, monga mtsogoleri wauzimu wa mpingo, mudzaona mochuluka momwe mpingo wanu umalandilira kutsanulidwa kwa Mzimu pamene kukubwera. Muyenera kutenga udindo wodabwitsawu mozama.

Chitsitsimutso cha Chipentekoste nthawi zambiri chimayamba ndi chikhumbo mu mtima wa abusa. Chikhumbo ichi cha kusuntha kwa Mzimu chidzamulimbikitsa iye kufunafuna Mulungu moona mtima kutsanulidwa kwa Mzimu Woyera pa mpingo. Kenako Mbusa ayenera kupereka chikhumbokhumbo chimenechi cha chitsitsimutso m’mitima ya anthu a Mulungu. Mungachite zimenezi polalikira ndi kuphunzitsa kawirikawiri pa mutuwo.

Mukhozanso kulenga chikhumbo choterocho m’mitima ya anthu anu powatsogolera m’mapemphero amphamvu a chitsitsimutso. Ponena za Mzimu

Woyera, Yesu anauza ophunzira ake kuti: "Ndinena ndi inu, Pemphani, ndipo adzakupatsani; funani, ndipo mudzapeza; gogodani ndipo adzakutsegulirani" (Luka 11:9; onaninso v. 13). Kumasulira kwenikweni kwa mawu a Yesu kunganenedwe motere, "Ndinena kwa inu: Pitirizani kupempha, ndipoadzakupatsani. Pitirizani kufunafuna, ndipo mudzapeza. Pitirizani kugogoda, ndipo khomo lidzatsegulidwa kwa inu." Tanthauzo lake ndi lomveka bwino: Pamene tipitirizabe kupempha Mzimu Woyera, tidzapitiriza kulandira kuchokera kwa Mulungu. Komabe, tikasiya kupempha, tidzasiya kulandira. Choncho, moto wa chitsitsimutso cha Pentekoste uyenera kuyatsidwa ndi kulimbikira kupemphera.

Komanso, monga Mbusa, muyenera kuwonetsa anthu anu momwe angapempherere ndi chikhulupiriro. Muyenera kuwatsogolera kuti akhulupirire kuti, ngati angafunefune Mulungu mokhulupirika, adzasunga lonjezo lake lotumiza chitsitsimutso (Marko 11:24). Mudzafuna mosalekeza kukumbutsa anthu za chilengezo chaulosi cha Petro: "Ndipo kudzali m'masiku otsiriza, anena Mulungu, *ndidzathira* cha Mzimu wanga pa thupi lililonse" (Machitidwe 2:17, kutsindika kwawonjezeredwa). Pamenemamembala a mpingo avomereza lonjezo limeneli, adzalimbikitsidwa kukhulupirira lonjezo la Yesu lakuti Atate wa Kumwamba "adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akumpempha Iye" (Luka 11:13).

Pamene mpingo ukutsata chitsitsimutso cha Chipentekoste, uyenera, nthawi yomweyo, kutsata ntchito ya Chipentekoste. Awa anali malangizo omveka bwino a Yesu pa Machitidwe 1:8. Choyamba, analonjeza chitsitsimutso: "Mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu." Pa nthawi yomweyo, Iye analamula ntchito: "Ndipo mudzakhala mboni zanga… mpaka kumalekezero a dziko lapansi."

Choncho, ngati Mbusa, ntchito yotsogolera okhulupirira ku ubatizo wa Mzimu Woyera pokonzekera umboni wa mphamvu ya Mzimu Woyera ikuyenera kukhala imodzi mwazofunikira zanu. Muyenera kukumbukira nthawi zonse kuti chifukwa chimodzi chachikulu chimene Mulungu anakuikani mu mpingo wanu ndikuti muwukitse ophunzira ena odzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu kuti awagwiritse ntchito pomanga ufumu wake (Aefeso 4:11-12).

KULIMBIKITSA CHITSITSIMUTSO CHA CHIPENTEKOSTE

Patangotha milungu yochepa kuchokera pamene Mzimu Woyera anatsanulidwa ku Yerusalemu pa Tsiku la Pentekoste, Malemba amanena za

kutsanulidwa kwina kumene kunachitika ku Samariya, pafupifupi makilomita 50 kumpoto kwa Yerusalemu (Mach. 8:1-25). Chitsitsimutsochi chinatsogozedwa ndi mlaliki Filipo mothandizidwa ndi mtumwi Petro ndi Yohane. Poona zochita za amunawa, tipeza njira zisanu ndi ziwiri zolimbikitsira chitsitsimutso mu mpingo:

Dzazidwani ndi Mzimu

Njira yoyamba yomwe inu, monga Mbusa wa Chipentekoste, mungalimbikitsire chitsitsimutso mu mpingo wanu ndi kufunafuna Mulungu moona mtima kuti mudzadzidwe kapena kudzazidwanso ndi Mzimu Woyera. Filipo anali mmodzi wa "wotumikira" (madikoni) asanu ndi awiri odzazidwa ndi Mzimu mu mpingo wa ku Yerusalemu (Mach. 6:3-5). Iye ayenera kuti anadzazidwa ndi Mzimu pa Tsiku la Pentekoste kapena posakhalitsa pambuyo pake. Pamene anathamangitsidwa m'mudzi ndi mazunzo, anakhalabe wodzala ndi Mzimu Woyera. Atafika ku Samariya, anatumikira mu mphamvu ya Mzimu, nayatsa chitsitsimutso champhamvu pamalopo.

Iye, pamodzi ndi mtumwi Petro ndi Yohane, amene anafika kuchokera ku Yerusalemu kudzam'thandiza (8:14-17), anakwanitsa kubweretsa chitsitsimutso mu Samariya chifukwa iwo eniwo anali odzala ndi mzimu woyera. Chitsitsimutso cha Chipentekoste chimayamba ndi inu, abusa, ndi atsogoleri ena ampingo kudzazidwa kapena kudzazidwanso ndi Mzimu Woyera.[1]

Onetsani Chikhulupiriro Cholimba

Njira yachiwiri yomwe mungalimbikitsire chitsitsimutso mu mpingo ndikukhala ndi chikhulupiriro cholimba. Filipo atafika ku Samariya, anachita zinthu mwa chikhulupiriro. Chotsatira chake, Mulungu adampatsa zozizwa kuti atsimikizire uthenga wake, ndipo ambiri adakopeka kwa Ambuye (Machitidwe 8: 5-8).

Mofanana ndi Filipo, muyenera kukhulupirira kuti chitsitsimutso n'chotheka. Muyenera kukhala otsimikiza kuti Mulungu ndi wokhoza kuchita zimene walonjeza (onani Aroma 4:18-21).

[1] Kuti mudziwe zambiri momwe abusa a Chipentekoste amakumanirana ndi Mzimu, onani Mutu 1: "Munthu Okumana Ndizochitika."

Ndipo muyenera kuchita molimba mtima malonjezo a Mulungu ndi chitsimikizo chonse kuti chitsitsimutso chikubwera. Ngati muchita izi, chikhulupiriro chanu chidzapatsirana. Pamene mamembala anu akuwona abusa awo akuchita ndi chikhulupiriro cholimba, iwonso adzalimbikitsidwa kukhulupirira Mulungu kuti awatsitsimutse.

Lengezani Khristu

Njira yachitatu yomwe mungatsogolere mpingo wanu ku chitsitsimutso cha Chipentekoste ndikulalikira uthenga wabwino wa Khristu mokhulupirika. Baibulo limatiuza kuti: "Filipo anatsikira kumzinda wina wa ku Samariya, nawalalikira iwo Khristu" (Mach. 8:5) Umu ndi mmene Akhristu ankachitira m'buku lonse la Machitidwe. Kulikonse kumene ankapita ankauza anthu za Yesu (Mach. 2:22; 3:13; 4:2, 33; 9:22; 16:31). Ngati mukufuna kukhala ndi chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano mu mpingo wanu, muyenera kuchita monga Filipo ndi atumwi adachitira. Muyenera kulalikira Khristu mokhulupirika kwa onse. Ndipo muyenera kuphunzitsa anthu anu kuchita zomwezo.[2]

Pemphererani Odwala

Chachinai, mukhoza kutsogolera mpingo wanu ku chitsitsimutso cha Chipangano Chatsopano popempherera mokhulupirika odwala ndi osautsika, kuyembekezera kuti Mulungu atsimikizire Mawu ake mwa uzimu ndi zizindikiro zozizwitsa zomwe zikutsatira. Ku Samariya, "makamuwo ndi mtima umodzi anasamalira zonenedwa ndi Filipo, pamene anamva, napenya zizindikiro zimene anazichita" (Mach. 8:6). Zizindikiro zozizwitsa zimenezi zinaphatikizapo maombolo amphamvu ndi machiritso ozizwitsa. Chotsatira chake, chisangalalo chachikulu chinadza kwa anthu, ambiri anapulumutsidwa, ndipo chitsitsimutso chinadza mu mzinda.[3]

---

[2] Kuti mudziwe zambiri pa nkhani ya kulalikira, onani Mutu 16: "Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu."

[3] Kuti mudziwe zambiri za utumiki mu zauzimu, onani buku la Chiyembekezo cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, Utumiki Wamphamvu: Mmene Mungatumikire mu Mphamvu ya Mzimu, lolembedwa ndi Denzil R. Miller, lopezeka ku Africa Theological Training Service (ATTS), https://africaatts.org/.

Tsindikani Za Ubatizo wa Mzimu

Njira yachisanu yomwe mungalimbikitsire chitsitsimutso cha Chipentekoste mu mpingo wanu ndikutsindika pafupipafupi kufunikira kwa anthu kuti abatizidwe ndi Mzimu Woyera. Atumwi ku Yerusalemu atamva kuti Asamariya alandira uthenga wabwino, nthawi yomweyo anatumiza Petro ndi Yohane kuti akapemphere nawo limodzi kuti alandire Mzimu Woyera (Mach. 8:14-17). Mbusa wa Chipentekoste aliyense amene akufuna kuti mpingo wake ukhale ndi chitsitsimutso chenicheni cha Chipentekoste ayenera kuchita chimodzimodzi. Ayenera kuphunzitsa ndi kulalikira kawirikawiri za ubatizo wa Mzimu. Ndipo ayenera kupemphera ndi anthu awo kuti alandire Mzimu. Izi zidzathandiza mpingo kukonzekera kutenga nawo mbali mokwanira pa chitsitsimutso ndi kufalitsa uthenga wabwino kwa otayika.[4]

Tsogolerani Mukuchitira Umboni

Njira yachisanu ndi chimodzi yomwe mungalimbikitsire chitsitsimutso cha Chipentekoste ndi kutsogolera mpingo wanu pochitira umboni kwa otayika. Filipo anayambitsa chitsitsimutso cha Asamariya kudzera mu umboni wolimba mtima wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu kwa anthu otayika a ku Samariya. Pochita izi, adakhala chitsanzo kwa mpingo. Tikudziwa kuti Akhristu atsopano a ku Samariya anatsatira chitsanzo chake pochitira umboni, chifukwa m'nthawi yochepa chabe "mpingo wa mu Yudeya yense ndi Galileya, ndi Samariya unali nao mtendere, nukhazikika; ndipo unayenda m'kuopa kwa Ambuye, ndi m'chitonthozo cha Mzimu Woyera, nuchuluka" (Mach. 9:31).

Inu monga Mbusa wa Chipentekoste, ngati mukufuna chitsitsimutso chenicheni cha uzimu mu mpingo wanu muyenera kutsatira chitsanzo cha Filipo. Musamangowauza anthu anu kuti achitire umboni, muyenera kukhala chitsanzo cha cholinga chenicheni cha chitsitsimutso cha Chipentekoste pokhala mboni nokha.[5]

---

[4] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kupemphera ndi okhulupirira kuti alandire Mzimu Woyera, onani Mutu 11: "Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekoste" ndi Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

[5] Kuti mudziwe zambiri za kutsogolera mpingo ku ulaliki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu, onani Mutu 36: "Kumvetsetsa Kachitidwe ka Zinthu M'chipangano Chatsopano" ndi Mutu 37: "Kulalikira Otayika."

Limbikirani Kupemphera

Pomaliza, mutha kutsogolera mpingo wanu ku chitsitsimutso cha Chipentekoste powonetsa mpingo momwe mungapempherere, monga tafotokozera kumayambiriro kwa mutu uno. Mtumwi Petro ndi Yohane atafika ku Samariya, "anapempherera [okhulupirira atsopano] kuti alandire Mzimu Woyera" (Machitidwe 8:15). Ngati mukufuna kuwona chitsitsimutso chenicheni cha Pentekoste chikubwera ku mpingo wanu, inunso muyenera kuwatsogolera anthu mu pemphero. Ndipo muyenera kulimbikira kupemphera mpaka yankho litafika, pokumbukira mawu a Paulo akuti: "Tisaleme pakuchita zabwino; pakuti pa nyengo yake tidzatuta tikapanda kufooka" (Agalatiya 6:9).[6]

Kuti ukhalebe umboni wofunikira mdera ndi pa dziko lapansi, mpingo uliwonse wa Chipentekoste uyenera kutsanulidwa mobwerezabwereza kwa Mzimu Woyera. Mbusa wa Chipentekoste ayenera kutsogolera ntchitoyi. Ayenera kupereka chitsanzo mwa kulondola chitsitsimutso ndi mtima wonse, ndipo ayenera kuphunzitsa anthu kuchita zomwezo. Iwo angalandire chilimbikitso kuchokera ku lonjezo la Mulungu kwa Yoweli logwidwa mawu ndi Petro pa Tsiku la Pentekoste:

"Ndipo kudzali m'masiku otsiriza, anena Mulungu, ndidzathira cha Mzimu wanga pa thupi lililonse, ndipo ana anu aamuna, ndi aakazi adzanenera, ndipo anyamata anu adzaona masomphenya, ndi akulu anu adzalota maloto; ndiponso pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m'masiku awa ndidzathira cha Mzimu wanga; ndipo adzanenera." (Machitidwe 2:17-18)

[6] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kutsogolera mpingo m'pemphero, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

~ Mutu 20 ~

Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu

Yesu anali pafupi kubwerera kumwamba. Ntchito imene anaiyambitsa anaisiyira ndi mpingo wake. Pokonzekera kunyamuka kwake, anasonkhanitsa ophunzira ake pamwamba pa phiri kunja kwa Yerusalemu. Pamenepo adawapatsa lamulo lomaliza ndi lonjezo lomaliza.

Lamulo lake linali lakuti, “Asachoke ku Yerusalemu, komatu alindire lonjezano la Atate, limene, anati, munalimva kwa Ine; pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri” (Machitidwe 1:4-5). Lonjezo lake linali lakuti, “Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko lapansi” (v. 8). Popereka malangizo amenewa, Yesu anali kusonkhanitsa mpingo wake womwe unali kubwera kuti ukwaniritse ntchito imene anawapatsa.

Mofanana, Mbusa aliyense wa Chipentekoste mu Afirika ayenera kulimbikitsa mpingo wake kuti uchite nawo ntchito ya chiombolo ya Khristu. Mofanana ndi Yesu, ayenera kuonetsetsa kuti anthu awo abatizidwa ndi Mzimu Woyera ndi kupatsidwa mphamvu monga mboni za Khristu kwa otayika. Palibe mpingo umene uli wokonzeka kutenga nawo mbali mokwanira mu utumiki wa

Mulungu kufikira atsogoleri ake ndi mamembala ake atalandira mphamvu yolonjezedwa imeneyi kuchokera kumwamba (Luka 24:49). Mutuwu ufotokoza za nkhani yofunikayi. Zidzakuthandizani kudzikonzekeretsa nokha kutsogolera mamembala anu ku ubatizo wa Mzimu Woyera.

KODI UBATIZO WA MZIMU WOYERA NDI CHIYANI?

Ubatizo wa Mzimu Woyera (omwe nthawi zina umatchedwa ubatizo wa Mzimu) ndizochitika zamphamvu zosintha moyo. Ndiko kukumana ndi Mulungu momwe Mzimu Wake amadza pa wotsatira Yesu, kuwaveka ndi kuwadzaza ndi kupezeka kwake ndi mphamvu zake. Ubatizo wa Mzimu Woyera ndi umene unachitikira ophunzira 120 pa Tsiku laPentekoste. Baibulo limafotokoza zochitika zawo motere:

> "Ndipo pakufika tsiku la Pentekoste, anali onse pamodzi pamalo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ochokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzadza nyumba yonse imene anali kukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga amoto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekhawayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa." (Machitidwe 2:1-4)

Taganizirani zimene zinachitikira ophunzira pa nthawiyo. Poyamba, Mzimu Woyera anadza pa iwo, monga mmene Yesu ananeneratu mu Machitidwe 1:8. Kenako, Mzimu analowa mwa iwo, kuwadzaza ndi mphamvu Zake zazikulu ndi kupezeka kwake.Chifukwa cha zimenezi, anayamba kulankhula malilime monga mmene Mzimu anawalankhulitsa. Potsirizira pake, anayamba kulalikira mwamphamvu ndi mogwira mtima (Machitidwe 2:14-41). Zimenezi zinapitirirabe m'buku lonse la Machitidwe. Ndipo tingayembekezere kupitiriza lero.

Poganizira zinthu izi, tikhoza kutsimikizira zinthu zitatu zokhudza ubatizo wa Mzimu Woyera:

1. Ndi chochitika champhamvu. Yesu anafotokoza ubatizo wa Mzimu Woyera kukhala "wovekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba" (Luka 24:49). Iye analonjeza kuti, "Mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu" (Mach.

1:8). Pamene munthu wadzazidwa ndi Mzimu, amakumana ndi mphamvu yaikulu ya Mulungu.

2. Ndilonjezo kwa okhulupirira onse. Yesu ananena kuti Atate wa Kumwamba adzapereka Mzimu Woyera kwaulere kwa mwana Wake aliyense amene angapemphe ndi chikhulupiriro (Luka 11:13; Marko 11:24). Mu ulaliki wake wa Pentekoste, Petro ananena za chochitikacho, "Lonjezo lili kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, kwa onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana" (Mach. 2:39).

3. Ndi lamulo lochokera kwa Mulungu. Yesu analamula ophunzira ake kuti: "Asachoke ku Yerusalemu, komatu alindire lonjezano la Atate, limene, anati, munalimva kwa Ine" (Machitidwe 1:4). Mofananamo, Paulo analangiza okhulupirira a ku Aefeso kuti "adzazidwe ndi Mzimu" (Aefeso. 5:18). Chifukwa Mkhristu aliyense wapatsidwa ntchito monga mboni ya Khristu, Mkhristu aliyense ayenera kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera (Luka 24:48-49; Machitidwe 1:8; 5:32).

Ubatizo waMzimu umathandizanso Mkhristu kukhala ndi moyo wokondweretsa Mulungu (Agal. 5:16). Kumakulitsa luso lake la kupemphera (Aroma 8:26-27). Ndipo ubatizo wa Mzimu umadza ndi kuthekera kokulirapo kwakuti munthu agwiritsidwe ntchito powonetsera mphatso za uzimu (1 Ako. 12:7-10). Kuwonjezera pamenepo, ubatizo wa Mzimu umatithandiza kukhala okhudzidwa kwambiri ndi zinthu za Mulungu (Yoh. 16:8; 1 Ako. 2:12), kuthekera kwa kumvetsa kokulirapo kwauzimu (Yoh. 3:8; 1 Ako. 2:14), chikondi cha pa Mulungu (Aroma 5:5), ndi kudzipereka kwakukulu ku ntchito yake (Machitidwe 4:20; 5:29). Mkhristu aliyense ayenera kubatizidwa ndi Mzimu Woyera.

KULIMBIKITSA UBATIZO WA MZIMU

Zinthu izi pokhala zoona, Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste adzagwira ntchito molimbika kudzoza ndi kutsogolera mamembala ake ku ubatizo wa Mzimu. Nazi njira zisanu zomwe mungagwiritse ntchito kulimbikitsa ndi kuthandiza anthu anu kuti abatizidwe ndi Mzimu Woyera:

1. *Athandizeni kumvetsa*. Choyamba, mukhoza kulimbikitsa anthu anu kudzazidwa ndi Mzimu powathandiza kumvetsetsa chikhalidwe, cholinga, ndi kufunika kwa zochitikazo. Mungachite zimenezi mwa kulalikira ndi kuphunzitsa

kawirikawiri pa nkhaniyo. Pamene okhulupirira adziwa zambiri za Mzimu, adzakhala okonzeka bwino kuyankha kwa Iye ndi kudzazidwa.[1]

2. *Limbikitsani khumbo.* Ponena za Mzimu Woyera, Yesu ananena kuti: "Ngati pali munthu wakumva ludzu, adze kwa Ine, namwe" (Yohane 7:37). Pa nthawi ina Iye analonjeza kuti: "Odala ali akumva njala ndi ludzu la chilungamo; chifukwa adzakhuta" (Mat. 5:6) Choncho, njala ndi ludzu la Mulungu ndi zofunika kwambiri kuti munthu alandire Mzimu Woyera.

Podziwa izi, mudzafuna kuyikiza mwa anthu anu chilakolako chofuna kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu wa Mulungu. Njira imodzi imene mungachitire zimenezi ndi kuwathandiza kuona m'maganizo mwanu mmene kudzazidwa ndi Mzimu kudzadalitsira miyoyo yawo. Madalitso amenewa akuphatikizapo mphamvu yochitira umboni, kuyenda pafupi ndi Khristu, kuthandizidwa m'pemphero, kupambana pa mayesero, ndi zina zambiri.

Mutha kukulitsanso chikhumbokhumbo cha Mzimu mu mitima ya anthu pakukhala moyo wodzazidwa ndi Mzimu patsogolo pawo. Pamene okhulupirira awona mphatso ndi chipatso cha Mzimu chowonekera m'moyo wa abusa awo, chilakolako chakudzazidwa ndi Mzimu chidzabadwa m'mitima yawo.

3. Limbikitsani chikhulupiriro. Apanso, polankhula za Mzimu, Yesu anati, "Iye amene wokhulupirira Ine…mitsinje ya madzi amoyo idzayenda kutuluka mkati mwake" (Yoh. 7:38). Paulo anafotokoza kuti, "tilandire lonjezano la Mzimuyo, mwachikhulupiriro" (Agal. 3:14). Popeza Mzimu amalandiridwa ndi chikhulupiriro, ndiye kuti mudzafuna kukonzekeretsa anthu anu kuti alandire Mzimuyo pomanga chikhulupiriro chawo mu malonjezano a Mulungu.

Mwachitsanzo, mungawakumbutse mawu a Khristu pa Luka 11. Pamenepo, Yesu analonjeza kuti, "Ndinena kwa inu: Pemphani, ndipo adzakupatsani…. Pakuti *yense* wakupempha alandira…" (vv. 9-10; fanizilani v. 13, kutsindika kowonjezera). Onetsani kuti aliyense mundimeyi akutanthauza mwana *aliyense* wa Mulungu— kuphatikiza iwo. Malonjezo ena amene mungawauze akupezeka pa Marko 11:24 ndi Machitidwe 2:39. Kuphatikiza apo, mutha kumanga

[1] Buku la *Kulengeza Pentekoste: Maulaliki 100 a Mphamvu ya Mzimu Woyera*, likupezeka pa webusayiti ya DecadeofPentecost.org. Likupezeka m'zinenero zambiri.

chikhulupiriro cha anthu pogawana nawo maumboni a iwo omwe Mulungu adawadzaza ndi Mzimu ndikuwagwiritsa ntchito ku ulemerero Wake.

Konzani nyengo yakupezeka kwa Mzimu. Njira ina yofunika imene mungathandizire anthu anu kudzazidwa ndi Mzimu Woyera ndiyo kukulitsa chikhalidwe choyenera mu mapemphero a mpingo. Ubatizo wa Mzimu umalandiridwa bwino mu chikhalidwe chomwe chikhulupiriro chiri chapamwamba ndipo kupezeka kwa Mzimu kumakhala kolimba. Chikhulupiriro chinganenedwe kukhala chapamwamba pamene anthu a Mulungu akuyembekezera mwachidwi kusuntha kwa Mzimu. Amayembekezera kuti Mulungu akwaniritsa malonjezo ake nthawi yomweyo. Kukhalapo kwa Mzimu kunganenedwe kukhala kwamphamvu pamene anthu azindikira kuyandikira kodabwitsa kwa Mulungu. Mofanana ndi Yakobo, angachitire umboni kuti, "Ndithu, Yehova ali mommuno" (Gen. 28:16).

Kumbukirani, pa Tsiku la Pentekoste, Mzimu Woyera poyamba anadzaza malowo; Kenako anadzaza anthu (Mach. 2:3-4). Choyamba, Kupezeka kwake kumamveka; ndiye, Mzimu amalandiridwa. Kukhalapo kwa Mzimu kungakulitsidwe kupyolera mu pemphero lochokera pansi pa mtima, kumvera Mawu, kupembedza kodzozedwa, ndi kumasuka kwa Mzimu.

5. Perekani mwayi. Pomaliza, ngati mukuyembekeza kuwona mamembala anu akubatizidwa ndi Mzimu Woyera, muyenera kuwapatsa mwayi wolandira pafupipafupi. Pemphero la Mzimu Woyera liyenera kukhala chochitika chokhazikika pamisonkhano yachipembedzo ya mpingo wanu. Kuphatikiza apo, muyenera kuyitanira kuguwa pafupipafupi komwe kumaphatikiza kuyitanira kuti mudzazidwe ndi Mzimu.

Pokonzekera mapemphero a mpingo wanu, muyenera kukhala ndi nthawi yokwanira kumapeto ndikuyitanira anthu ku guwa kuti apemphere. Izi zingatanthauze kuti mufunika kufupikitsa kulambira ndi nthawi yolalikira. Kupitilira apo, mudzafuna kuphunzitsa ogwira ntchito kugome momwe angatsogolere ofunafuna ku ubatizo wa Mzimu. Kuonjezera apo, mungafune kukonza misonkhano ya mapemphero ndi milaga kuti okhulupirira athe kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu.

KUPEMPHERA NDI OKHULUPIRIRA KUTI ALANDIRE

Mwapereka ulaliki wanu, ndipo okhulupirira adziwonetsera okha kuti afunika adzazidwe ndi Mzimu. Ndiye muyenera kuchita chiyani? Kodi mungawatsogolere bwanji ofunafunawa mu ubatizo wa Mzimu Woyera?

Choyamba, ndikofunikira kuti mudziwe za uzimu zomwe zikuyenera kuchitika m'miyoyo ya okhulupirira awa pamene akudzazidwa ndi Mzimu. Monga pa Tsiku la Pentekoste, Mzimu adzayamba kudza pa iwo (Mach. 2:3). Kenako adzathamangira mkati mwawo, kuwadzaza ndi mphamvu ndi kupezeka Kwake (v. 4a). Pomaliza, Mzimu adzatuluka mwa iwo mu mawu owuziridwa ndi Mzimu (v. 4b). Muyenera kuyang'ana mphamvu za uzimu izi kuti zichitike mwa okhulupirira pamene akubatizidwa mu Mzimu Woyera.

Muyeneranso kukumbukira mfundo yakuti, pa nthawi yonseyi, ofunafuna adzafunika kuchita zinthu molimba mtima (Agal. 3:2, 5, 14). Kumbukirani, ndi chikhulupiriro chimene chidzakonzekeretsa mitima yawo kulandira Mzimu; ndi chikhulupiriro chimene chidzabweretsa kukhalapo Kwake; ndipo ndi chikhulupiriro chimene chidzamasula mphamvu ya Mzimu mu mawu owuziridwa. Ndi zinthu izi m'maganizo, tiyeni tione m'mene inu, monga Mbusa wa Chipentekoste, mungatsogolere ofunafuna ku ubatizo wa Mzimu.

Njira Zitatu Zachikhulupiriro

Pa Luka 11:9-13, Yesu akuphunzitsa ophunzira ake mmene angapemphere ndi kulandira Mzimu Woyera. Ndimeyi, pamodzi ndi zimene zinachitikira atumwi 120 pa Tsiku la Pentekoste (Mach. 2:1-4), zikusonyeza chitsanzo cha njira zitatu za kulandira Mzimu Woyera. Njira zitatuzi ndikupempha ndi chikhulupiriro, kulandira mwa chikhulupiriro, ndi kulankhula ndi chikhulupiriro. Umu ndi momwe mungatsogolere ofunafuna munjira zitatu izi zachikhulupiriro:

Njira 1: Pemphani ndi chikhulupiriro. Choyamba, atsogolereni ofuna kupempha Mzimu. Kumbukirani lonjezo la Yesu lakuti: "Pemphani, ndipo adzakupatsani" (Luka 11:9). Monga momwe mungatsogolere wochimwa m'pemphero la wochimwayo, mukhoza kutsogolera ofunafunawo m'pemphero lopempha kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Alangizeni kuti pamene akupemphera, ayenera kukhulupirira mozindikira kuti Mulungu akumva pemphero lawo ndi kuti akuchitapo kanthu kuti ayankhe pemphero lawo. Pempheroli likhoza kupitilira motere, ndi ofuna kubwereza mzere uliwonse:

> "Ambuye, ndabwera kuti ndidzadzidwe ndi Mzimu Woyera… Munalonjeza kuti ndidzalandira mphamvu pamene Mzimu adzadza pa ine... Ine ndikufuna mphamvu imeneyo kuti ndikhale mboni yanu… Munalonjezanso kuti aliyense amene apempha amalandira… Ndikukupemphani; choncho, Inendikuyembekezera kulandira…Pamene ine ndilandira, ine ndidzayankhula momveka mwa chikhulupiriro... Sindidzawopa…Ine ndidzayamba kuyankhula mu malilime pamene Mzimu Wanu akundipatsa ine zolankhula…Mzimu Woyera, bwerani pa ine tsopano."

Mukangopemphera, atsimikizireni oyembekezera kuti Mulungu wamva pemphero lawo, ndipo ali wokonzeka tsopano kuwadzaza ndi Mzimu Woyera. Alimbikitseni kukhala okhudzidwa ndi kubwera kwa Mzimu pa iwo. Ayenera kuzindikira kukhalapo Kwake. Mungafune kutenga kamphindi pang'ono kuti mupembedze Ambuye pamodzi, kuyankha pa kubwera kwa Mzimu.

Njira 2: Kulandira mwa chikhulupiriro. Tsopano, atsogolereni ofunafuna mu mayendedwe awo a chikhulupiriro. Yesu anati: "Yense wakupempha *alandira*" (Luka 11:10, kutsindika kwaonjezeredwa). Yesu akunena za kulandira mwachidwi osati kungolandira chabe. Iye akunena kuti, "Yense amene apempha ayenera kufikirapo kuti alandire." Yesu anatiuza mmene zimenezi zimachitikira. Zimachitika ndi ntchito ya chikhulupiriro. "Zinthu zilizonse mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupirirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala nazo" (Marko 11:24).

Kuti mutsogolere ofunafunawo m'njira yawo ya chikhulupiriro, afunseni kukweza manja awo kumwamba, ndipo mwa chikhulupiriro pempherani pemphero losavuta ili: "Ambuye, tsopano lino, m'dzina la Yesu, ndilandira Mzimu Woyera." Pempheroli lidzawapatsa mfundo yotsimikizika pamene angamasulire chikhulupiriro chawo kuti alandire Mzimu. Panthawiyo, ayenera "kukhulupirira kuti alandira!" Nthawi yomwe akhulupirira, Mzimu amathamanga mwa iwo ndi kuwadzaza. Auzeni kuti azindikire kupezeka kwa Mzimu mkati mwao.

Njira 3: Kulankhula mwachikhulupiriro. Tsopano, alimbikitseni ofunawo kuchita zinthu mwachikhulupiriro ndikuyamba kulankhula molimba mtima—osati kuchokera m'maganizo mwawo, koma kuchokera pansi pamtima, kumene amaona kukhalapo kwa Mulungu mkati mwake (Yohane 7:38). Pamene akudzipereka ku Mzimu akuyenda mkati mwa umunthu wawo, adzayamba kulankhula mawu omwe sakuwamva (Machitidwe 2:4; 10:46; 19:6). Kulankhula

kwawo kungayerekezedwe ndi njira ya chikhulupiriro ya Petro pamene, momvera lamulo la Yesu, anatuluka m'ngalawamo nayamba kuyenda pamadzi. Khalidwe lake lolimba mtima lachikhulupiriro linabweretsa chozizwitsa (Marko 14:28-29). Nawonso adzatero! Alimbikitseni kuti asakhale amantha koma kuti agwirizane ndi Mzimu kwathunthu popitiriza kulankhula ndi chikhulupiriro.

Kuyankhula mu Malilime

Kungakhale kothandiza pano kunena zochulukira ponena za kulankhula m'malilime, popeza kuti ichi kawirikawiri chilichochitika chatsopano ndipo mwinamwake chachilendo kwa awo amene sanachionepo. Ndikofunikira kumvetsetsa kuti, pamene wokhulupirira wodzazidwa ndi Mzimu alankhula m'malilime, mawu amene amalankhula samatuluka m'maganizo mwawo, monga m'mawu achibadwa. Mawuwa amachokera pansi pamtima, kuchokera ku mizimu yawo. Yesu anati: "Iye wokhulupirira Ine, monga Chilembo chinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda kutuluka m'kati mwake" (Yoh. 7:38). Paulo anati: "Iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibe munthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi" (1 Ako. 14:2). Akumbutseni ofunafunawo kuti kulankhula kwawo sikukakamizika. Kudzakhala kuyenda kwachibadwa kwa mawu auzimu. Ayenera kungolola kuti zichitike, ndi kugwirizana ndi Mzimu polankhula molimba mtima ndi chikhulupiriro.

Uphungu Wotsatira Pambuyo Pa Pemphero

Ndikofunikira kuti uphungu wa pambuyo pa pemphero uperekedwe kwa ofuna kubatizidwa. Ngati adadzazidwa ndi Mzimu, mudzapereka uphungu wamtundu umodzi; ngati sanadzadzidwe, mudzapereka uphungu wa mtundu wina.

Kwa iwo amene ali odzazidwa ndi Mzimu ndi kulankhula malilime, perekani uphungu uwu: Muwawuze iwo kuti kulandira Mzimu sizikungothera pompo; koma ndi njira yokathera kuchinthu chachikulu. Cholinga cha kulandira kwawo Mzimu ndi kuti alandire mphamvu zakukhala moyo wa Mulungu ndi kukhala mboni zopatsidwa mphamvu za Khristu. Mudzafunanso kuwalimbikitsa kukhala ndi nthawi tsiku lililonse kupemphera mu Mzimu, ndiko kuti, kupemphera m'malilime. Mchitidwe umenewu udzawalimbitsa mwauzimu, ndipo udzawakumbutsa za kupezeka kwa Mzimu mkati (1 Ako. 14:4).

Kwa amene pa nthawi ino, sanadzadzidwe ndi Mzimu, perekani uphungu uwu: Auzeni kuti asataye mtima, ndipo atsimikizireni kuti lonjezo la Yesu likadali

loona: "Pemphani, ndipo *adza*kupatsani" (1 Yoh. Luka 11:9, kutsindika kwawonjezeredwa). Auzeni kutiazipemphabe, kufunafuna, ndi kugogoda, monga momwe Yesu anaphunzitsira. Pamene akutero, ayenera kukumbukira lonjezo la Yesu lakuti: "*Yense* wakupempha alandira" (v. 10, kutsindika kwawonjezeredwa). Mungafune kuwafunsa ngati akufuna kupempheranso. Ngati atero, bwerezani zimene zili pamwambazi, ndi kuwalimbikitsa kuchita zinthu molimba mtima.

KULIMBIKITSA AMENE AKULANDIRA

Monga Mbusa wa Chipentekoste, musaiwale chifukwa chachikulu chimene Yesu amabatizira otsatira ake ndi Mzimu Woyera. Amawabatiza kuti awapatse mphamvu monga mboni zake (Machitidwe 1:8). Muyenera kulimbikitsa iwo amene adadzazidwa ndi Mzimu Woyera kuti ayambe kuchitira umboni kwa mabanja awo ndi anzawo. Muyeneranso kuwatsogolera ku uvangeli wolimba mtima, kudzala mipingo, ndi utumwi. Izi ndi zimene Yesu ndi atumwi anachita mu Mauthenga Abwino ndi m'buku la Machitidwe.[2]

Yesu atangodzozedwa ndi (kubatizidwa) ndi Mzimu Woyera, anayamba kutumikira mu mphamvu (Luka 3:22-23; 4:8; 14, 18-19; 5:17). Atalandira Mzimu pa Tsiku la Pentekoste, Petro anayimirira pamodzi ndi ophunzira ndi kulalikira ndi mphamvu kotero kuti anthu zikwi zitatu anadza kwa Ambuye (Machitidwe 2:14-41). Iwo amene anabwera kwa Khristu anachitiranso umboni ndi mphamvu.Chifukwa cha umboni wawo, "Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akupulumutsidwa" (v. 47). Patapita masiku angapo, pamene Mulungu anatsanuliranso Mzimu Wake pa ophunzira ku Yerusalemu, "anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula mawu a Mulungu molimbika mtima" (4:31). Mchitidwe umenewu unapitirirabe m'buku lonse la Machitidwe a Atumwi, ndipo uyenera kupitirirabe m'mipingo yathu ya Chipentekoste masiku ano.

[2] Kuti mudziwe zambiri pa nkhani zimenezi, onani, Mutu 37: "Kulalikira Otayika" ndi Mutu 39: "Kudzala Mipingo Yatsopano."

~ Mutu 21 ~

Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu

Henry ndi mkazi wake Ruth anali kutumikira monga atumwi kwa anthu olambira mafano a m'mudzi wa Glofaken kum'mwera chakum'mawa kwa Liberia. Kwa nthawi yaitali, Henry analikulimbikitsa anthu kuti asiye mafano awo ndi kutembenukira kwa Yesu, koma ndi ochepa okha amene analabadira.

Tsiku lina, mfumu ya mudziwo ndi akulu ake anapita kwa Henry. Mkuluyo anauza Henry kuti: "Iwe wakhala ukutikakamiza kuti tisiye mafano a makolo athu n'kutembenukira kwa Mulungu wako. Mukunena kuti Mulungu wanu ndi wamphamvu kuposa mafano athu, koma sitinaone mphamvu ya Mulungu amene mumanyadira. Ngati mungationetse mphamvu zake, tiganizira zoleka wathuyu kuti timutumikire wanuyo."

Henry ankadziwa kuti mkuluyo sanali kungomutsutsa; anali kutsutsa Mulungu! Chotero Henry anapemphera, "Ambuye, onetsani mphamvu Yanu kwa anthu aku Glofaken." Mulungu anayankha pemphero la Henry, ndipo posakhalitsa anayamba kusonyeza mphamvu zake kudzera mu utumiki wa Henry.

Tsiku lina m'mawa, mwana wa mfumuyo anapempha Henry kupemphera kuti Mulungu amuchotsere ng'ala imene inaphimba maso ake, kuti asaone bwino. Henry anasanjika manja ake pamunthuyo ndi kupemphera, kupempha Mulungu kuti amuchitire chozizwitsa. Nthawi yomweyo Mulungu anayankha pemphero lake, ndipo ng'ala ya munthuyo inasowa!

Pambuyo pake, Mulungu anapitiriza kuchita zozizwitsa pakati pa anthu a ku Glofaken. Panthawi ina, Mulungu analankhula ndi Henry kumuuza kuti aike manja pa mkazi wakufa amene anali pafupi kuikidwa m'manda. Modabwitsa anthuwo, maso a mkaziyo anatseguka, ndipo moyo wake unabwezeretsedwa. Pazifukwa izi ndi zozizwa zomwe zinachitika, Amfumu ndi nduna zake adatembenukira kwa Mulungu, nakhulupirira Yesu, pamodzi ndi anthu ena ambiri a mudzi wa Glofaken. Mpingo wamphamvu wodzazidwa ndi Mzimu unakhazikitsidwa.

Mu Kutumidwa Kwakukulu, Yesu analamulira Mpingo Wake, "Mukani kudziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. Amene akhulupirira nabatizidwa, adzapulumutsidwa, koma amene sakhulupirira adzalangidwa." Pa lamulo limeneli Iye anawonjezera lonjezo: "Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo akukhulupirira: m'dzina langa adzatulutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja awo pa odwala, ndipo adzachira" (Marko 16:15-18). M'mbiri yonse ya Mpingo, anthu akhala akukhulupirira Yesu pamene anamva uthenga wabwino ndi kuchitira umboni mphamvu ya Mzimu Woyera.

Mutu uwu ufotokoza kufunika kwa mbusa wa Chipentekoste kutumikira mu mphamvu ya Mzimu. Pochita izi, tidzayang'ana pa mphatso zowonetsera zomwe zalembedwa mu 1 Akorinto 12:8-10, pamodzi ndi cholinga chawo mu utumiki. Tidzaperekanso malangizo a m'Baibulo a kagwiritsidwe ntchito ka mphatso zauzimu mu mpingo.

UTUMIKI MU MPHAMVU YA MZIMU

Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kudziwa momwe angatumikire mu mphamvu ya Mzimu ndi zizindikiro zotsata. Utumiki woterewu unali chizolowezi cha utumiki mu Chipangano Chatsopano, ndipo ukadali chizolowezi cha utumiki lero.

Utumiki wa mphamvu umachokera mu Mzimu wa Mulungu. Choncho n'zomveka kunena kuti aliyense amene akufuna kutumikira mu mphamvu ya Mzimu ayenera kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Yesu anamvetsa zimenezi. N'chifukwa chake asanakwere kumwamba, anasiyira ophunzira ake lamulo lomaliza lakuti: "Asachoke mu Yerusalemu, komatu alindire lonjezano la Atate, limene, anati, munalimva kwa Ine; pakuti Yohane anabatizadi ndi madzi; koma

inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera, asanapite masiku ambiri" (Mach. 1:4-5). Pamenepo Yesu anawalonjeza kuti, "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko" (v. 8).

Zachisoni, abusa ambiri mu Afirika lero sanalandire mphamvu ya Mzimu. Chifukwa amuna ndi akazi awa sali odzazidwa ndi Mzimu Woyera, samawona chiwonetsero cha mphamvu ya Mzimu mu mautumiki awo. Izi ndi zomvetsa chisoni. Ngati simunadzadzidwe ndi Mzimu Woyera, muyenera kufunafuna Mulungu mpaka "muvekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba" (Luka 24:49). Mulungu adzakudzadzani ndi Mzimu ndi kukupatsani mphamvu ya utumiki, monga anachitira ophunzira oyambirira aja pa Tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2:1-4).[1]

Kupitilira apo, pali abusa a Chipentekoste omwe, ngakhale adadzazidwa ndi Mzimu, amaonetsera mphamvu zochepa chabe za Mzimu muutumiki wawo. Ambiri mwa azibusawa amaganiza kuti cholinga chokha chodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndicho kuwapangitsa iwo kulankhula malilime. Iwo ali ngati mlenje wa m'mudzi amene amatsuka mfuti yake m'mawa uliwonse, kuwombera mfuti pang'ono m'mwamba, kuiika pambali, ndi kuyembekezera kuti mkazi wake aphike nyama yabwino. Amapanga phokoso lambiri, koma amakwaniritsa zochepa kwambiri.

Ngakhale kuyankhula m'malilime ndi chionetsero chofunikira cha Mzimu, sicholinga choyambirira chakudzazidwa ndi Mzimu. Cholinga choyambirira chakudzazidwa ndi Mzimu ndikupatsidwa mphamvu ya utumiki (Mach. 1:8). Monga abusa a Chipentekoste, tiyenera kupitilira pamlingo wakungoyankhula ndi malilime nkufika ku utumiki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu. Tiyenera kuphunzira kutumikira mu mphamvu ya Mzimu pamodzi ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Utumiki woterewu udzabweretsa madalitso kwa anthu a Mulungu ndi kukokera ochimwa kwa Yesu.

[1] Kuti mudziwe zambiri pa nkhaniyi, onani Mutu 2: "Munthu wa Mzimu" ndi Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

ZITSANZO ZA UTUMIKI WA MPHAMVU YA MZIMU OYERA

Mbusa wa Chipentekoste angaphunzire bwino momwe angatumikire mu mphamvu ya Mzimu pophunzira ndi kutsanzira utumiki wa Yesu mu Mauthenga Abwino ndi ophunzira oyambirira mu buku la Machitidwe.

Utumiki Wa Yesu Khristu

Ngakhale kuti Yesu analidi Mulungu owonekera mu thupi, anasankha kukwaniritsa utumiki wake monga munthu wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Baibulo limati iye "anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu" (Afilipi 2:7). Motero Yesu anakhala chitsanzo chathu chachikulu cha utumiki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu.

Zaka mazana ambiri Yesu asanabwere, Yesaya ananeneratu kuti Mesiya adzakwaniritsa kuitanidwa kwake mu mphamvu ya Mzimu Woyera (Yesaya 61:1-2). Pokwaniritsa ulosi wa Yesaya, Yesu anayamba utumiki wake wapadziko lapansi mwa kulengeza kuti: "Mzimu wa Ambuye uli pa ine, chifukwa Iye wandidzoza ine kulalikira Uthenga Wabwino" (Luka 4:18). Pamene Yesu analosera za ulosi wa Yesaya, iye anayamba utumiki wake wapadziko lapansi. Petro anafotokoza utumiki wa Yesu wa ku Nazarete ndi mphamvu ya Mzimu: "Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza Iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nachita zabwino, nachiritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi Iye" (Mach. 10:38). Ndime izi ndi zina mu Chipangano Chatsopano zikusonyeza kuti Yesu anachita utumiki wake mu mphamvu ya Mzimu Woyera (onani Luka 4:1, 14; 5:17). Zozizwitsa, zizindikiro, ndi zodabwitsa zimene zinatsagana ndi utumiki wa Yesu zinathandiza kukhutiritsa anthu kumtsatira Iye (onani Mateyo. 4:23-25; 9:35-36; Yohane. 2:11).

Kudalira mwaufulu kwa Ambuye wathu pa mphamvu ya Mzimu mu utumiki kumatipatsa chitsanzo chabwino. Mofanana ndi Yesu, tiyenera kupatsidwa mphamvu ndi mzimu woyera, ndipo mofanana ndi iye, tiyenera kulengeza uthenga wabwino molimba mtima kwa anthu onse. Pa nthawi yomweyo, tiyenera kukhulupirira Mulungu kuti adzatsimikizira mawu olalikidwa ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zochitidwa mu mphamvu ya Mzimu Woyera.

Utumiki wa Atumwi

Pamodzi ndi utumiki wa Yesu, utumiki wa atumwi ndi ophunzira ena m'buku la Machitidwe umatipatsa zitsanzo zabwino kwambiri za utumiki mu mphamvu

ya Mzimu. Ophunzira oyambirirawa anaphunzira kutumikira mu mphamvu ya Mzimu poyang'ana ndi kutsanzira utumiki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu wa Yesu.Pafupifupi chozizwitsa chilichonse chimene ophunzira anachita m'buku la Machitidwe chimachokera ku chozizwitsa chimene Yesu anachita m'mauthenga abwino.

Atumwi anatsatira chitsanzo cha Yesu cha kudzazidwa ndi Mzimu. Iwo ankadziwa kuti, asanatumikire monga mmene Iye ankachitira, ankafunika kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu monga mmene Iye anachitira. Ndipo mofanana ndi Yesu, iwo anaonetsetsa kuti onse amene anabwera kwa Khristu amapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera ndi kutsogozedwa kuchita utumiki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu (onani Machitidwe 2:38-39; 8:14-17; 9:17; 19:1-7)**.**

Zitsanzo izi zikutiphunzitsa kuti utumiki woona wa Chipangano Chatsopano umaposa chidziwitso cha chilengedwe, luso, ndi kuthekera kwathu. Zimafunika mphamvu ya uzimu, imene imadza pakudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Pansi pa kudzozedwa kwa Mzimu Woyera, Yesu ndi atumwi analengeza uthenga wa chipulumutso ndi zizindikiro zowatsatira.

CHOLINGA CHA ZIZINDIKIRO NDI ZODABWITSA

Nanga ntchito ya zizindikiro ndi zodabwitsa mu utumiki wa uthenga wabwino ndi chiyani masiku ano? Zizindikiro, zozizwa, ndi zozizwitsa zimasonyeza chifundo chachikondi cha Mulungu pa anthu ochimwa. Zimasonyeza kuti uthenga wabwino uli ndi mphamvu yosintha miyoyo. Mofanana ndi zikwangwani za m'misewu, zimalozera anthu kwa Yesu monga Mchiritsi, Momboli, ndi Mpulumutsi. Yohane akutiuza kuti: "Khamu lalikulu la anthu linamtsata [Yesu] Iye, chifukwa anaona zizindikiro zimene anachita pa odwala" (Yohane. 6:2; onaninso Yohane 20:30-31; Machitidwe 3:1-10). Mulungu akufuna kuti zomwezo zichitike muutumiki wathu lero.

Yesu ananenanso kuti zipata za gehena, zoyendetsedwa ndi ziwanda, sizingagonjetse mpingo wake kupita patsogolo (Mat. 16:18). Anatulutsa ziwanda kuti amasule oponderezedwa ndi kuonetsa ulamuliro wa ufumu wake pa ufumu wa mdierekezi(Mat. 12:28-29; Luka 11:20-22). Yesu wapereka mphamvu ndi ulamuliro womwewu kwa onse amene adzalandira Mzimu Wake ndi kudzipereka okha ku ulamuliro Wake (Mat. 10:1; Marko 3:14-15; Luka 9:1-2; Mach. 1:8).

Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuzindikiranso kuti mphamvu ya Mzimu ilipo kwa membala aliyense wa mpingo wake (Mach. 2:39). Mulungu akufuna kudzaza aliyense wa iwo ndi Mzimu Wake Woyera, kuwapatsa mphamvu yakuchitira umboni, ndi kuwapatsa mphatso zosiyanasiyana za Mzimu. Amachita zimenezi "kuti apindule nao" ku mpingo (1 Ako. 12:7) ndiponso kuti ufumu wake upite patsogolo padziko lapansi (onani Marko 16:20).[2]

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Mphamvu ya Mzimu Woyera yolandiridwa pa ubatizo wa Mzimu imamasulidwa mu utumiki makamaka kudzera mu mawonetseredwe a mphatso zauzimu. Pa 1 Akorinto 12:8-10, Paulo akulankhula za mphatso zisanu ndi zinayi za Mzimu zomwe ziyenera kugwira ntchito mu mpingo uliwonse. Mphatso zisanu ndi zinayi zimenezi nthawi zina zimatchedwa mphatso *zachionetsero*, popeza kuti, m'ndime 7, Paulo akuzitchula kukhala "machitachita a Mzimu." Mphatso izi zatanthauzidwa ngati kudzoza kwa uzimu koperekedwa ndi Mzimu Woyera kudzera mwa ophunzira odzazidwa ndi Mzimu kuti akwaniritse chifuniro cha Atate. Mphatso zisanu ndi zinayi zowonetsera zikhoza kugawidwa m'magulu atatu: Gulu loyamba ndi mphatso za *mavumbulutso*, ndipo likuphatikizapo mau a chidziwitso, mau a nzeru, ndi kusiyanitsa pakati pa mizimu. Gulu lachiwiri ndi mphatso *zauneneri*, ndipo zimaphatikizapo uneneri, malilime amitundumitundu, ndi kumasulira malilime. Gulu lachitatu ndi mphatso za *machitidwe amphamvu*, ndipo limaphatikizapo mphatso za machiritso, chikhulupiriro, ndi mphamvu zozizwa. Ndi makamaka kudzera mu mphatso za mphamvu kuti zizindikiro ndi zodabwitsa zimawonetseredwa.[3]

Cholinga cha Mphatso Zauzimu

Mzimu amapereka mphatso za uzimu pazifukwa zitatu: Choyamba, amazipereka kumangirira, kapena kuwumba mpingo (1 Akorinto 12:7; 14:12, 26). Chifukwa cha kulimbikitsidwa, mpingo ukhoza kukonzekeretsa mamembala ake kuti agwire ntchito (Aefeso. 4:11-12).

---

[2]Mutha kupeza zambiri za kutsogolera mamembala ampingo kuti adzazidwe ndi Mzimu mu Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

[3]Kuti mupeze mndandanda wathunthu wa mphatsozi limodzi ndi matanthauzo ndi zolinga zake, onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

Chachiwiri, Mzimu amapereka mphatso kuti mpingo ufalitse uthenga wabwino kwa otayika. Ntchito imeneyi ya mphatso za uzimu ikuwonetsedwa mu buku la Machitidwe pamene mphatso zimaonekera patsogolo pa ulaliki ndi utumwi**.**

Pomaliza, Mzimu Woyera amapereka mphatso za uzimu kuti mpingo ukule ndi kudzala mipingo yodzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Ndikosavuta kukhazikitsa mpingo kumene uthenga wabwino ukulalikidwa ndi zizindikiro zotsatira kuposa pamene palibe mawonetseredwe a mphamvu ya Mulungu. Nkhani ya Henry ndi Ruth, imene yafotokozedwa kumayambiriro kwa mutu uno, ikusonyeza mfundo imeneyi.

Ntchito ya Mphatso Zamzimu

Mphamvu ya uzimu ndiyofunikira kuti mpingo ugwire bwino ntchito. Komabe, mphamvu yauzimu ingagwiritsidwe ntchito molakwika. Monga mmene mkulu wa boma angagwiritsile nchito molakwika mphamvu zandale, Mkhristu wa Chipentekoste angagwilitsile nchito molakwika mphamvu zauzimu. Kuti tipewe izi, mu 1 Akorinto 12-14 Paulo adapereka malangizo a kagwiritsidwe ntchito koyenera kwa mphatso za uzimu mu mpingo.

M’mutu 13, mtumwi akunena kuti mphatso zauzimu ziyenera kuzindikiridwa monga zisonyezero za chikondi cha Mulungukupyolera mwa wokhulupirira. Kudera nkhawa kwachikondi pa ubwino wa ena kuyenera motero kukhala mfundo imene imatsogolera mawonetseredwe aliwonse a Mzimu.

Kenako, m’mutu 14, Paulo akuika malamulo ena ofunikira kwambiri amawonetseredwe oyenera a mphatso za Mzimu Woyera mumpingo wapamalo, makamaka mphatso za kunenera, malilime, ndi kumasulira malilime. Iye akuti mau aulosi sayenera kuyambitsa chisokonezo mu mpingo. Ayenera kutumikira kumangilira,kulimbikitsa, ndi kutonthoza anthu a Mulungu (v. 3). Kuonjezera apo, mphatso zauneneri ziyenera kuperekedwa nthawi zonse mwadongosolo (vv. 27-32). Ndipo potsiriza, mzimu ndi zomwe zili m'mau aulosi ziyenera "kuyesedwa mosamala" ngati zikuchokera kwa Mulungu zisanalandiridwe (v. 29).

Masiku ano ku Afirika konse, mphatso zauneneri komanso mphatso zamphamvu zikugwiritsiridwa ntchito molakwika. Aneneri onyenga ndi atumwi onyenga asandutsa machiritso ndi zozizwitsa kukhala ntchito yopezera phindu. Amuna ndi akazi achinyengo amenewa mopanda manyazi amagulitsa zizindikiro

ndi zodabwitsa zawo zabodza kwa anthu amene amafuna njira zothetsera mavuto awo. Komabe, m'Malemba onse, palibe chozizwitsa chimene chimagulitsidwa kwa aliyense.

Monga Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste, muyenera kuonetsetsa kuti mpingo wanu usatsatire makhalidwe oipawa. M'malo mwake, muyenera kudalira Mulungu modzichepetsa kuti achite zizindikiro ndi zodabwitsa kudzera muutumiki wanu. Ndipo muyenera kuchita izi popanda kugonjera ku chiyeso cha kugulitsa zozizwitsa za Mulungu. Yesu analamula ophunzira ake kuti: "Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, tulutsani ziwanda." Kenako anawonjezera kuti: "Munalandira kwaulere; patsani kwaulere" (Mateyu 10:8). Mbusa wa Chipentekoste amakumbukira nthawi zonse kuti mphatso zauzimu sizili zake kuti azigwiritsa ntchito momwe angafunire. M'malo mwake, ndi mphatso za Mzimu Woyera ndipo ziyenera kugwiritsidwa ntchito "monga momwe wafunira" (1 Ako. 12:11).

Mutha kuwunika mawonekedwe a mphatso ya uzimu mu mpingo pofunsa mafunso awa:

1. Kodi mawonetseredwewa akugwirizana ndi Mau a Mulungu? Ngati sizikugwirizana ndi ziphunzitso zomveka bwino za m'Malemba, ziyenera kukanidwa. Mzimu wa Mulungu sadzatsutsana ndi Mawu a Mulungu.

2. Kodi mawonetseredwe a mphatso amalemekeza Mulungu? Mphatso zauzimu sizimaperekedwa kuti zikweze mtumiki; zimapatsidwa kulemekeza Mulungu ndi kulozera anthu kwa Yesu (Mat. 15:31; Marko 2:12). Ngati kuwonetseredwa kwa mphatso ya uzimu kumakweza wina aliyense kupatula Mulungu, ziyenera kukayikiridwa (Yoh. 16:13-15; 1 Ako. 1:29).

3. Kodi mawonetseredwe amangirira mpingo? Mphatso zauzimu zimaperekedwa kuti zimange mpingo. Ngati chiwonetsero chimayambitsa chisokonezo kapena kufooketsa chikhulupiriro cha anthu mwa Khristu, chiyenera kukanidwa.

4. Kodi mawonetseredwewa amathandiza kupititsa patsogolo ntchito ya Mulungu? Mphatso za uzimu ndi zida zamphamvu za kulalikira ndi kudzala mipingo. Choncho, iwo amene akugwira ntchito mu mphatso ayenera kukhala mboni zogwira mtima za Khristu. Ngati mawonetseredwe a Mzimu amasokoneza kapena kutembenuza anthu kuchoka ku ntchito ya Mulungu, sikuyenera kuloledwa.

Kulimbikitsa Mphatso Zauzimu

Pamene inu, ngati Mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kusamala kuti musagwiritse ntchito molakwika mphatso za uzimu mu mpingo wanu, ichi chisakhale chokhumba chanu chachikulu.Cholinga chanu chachikulu chikhale kulimbikitsa mawonetseredwe a mphatso. Simuyenera kukhutitsidwa ndi zokambirana chabe za zizindikiro ndi zodabwitsa. M'malo mwake, muyenera kuwalimbikitsa kuti azigwira ntchito pafupipafupi mu mpingo ndi pamsika. Mutha kuchita izi m'njira zinayi*:*

Choyamba, muyenera kuphunzitsa mamembala anu za chisamaliro chachikondi cha Mulungu kwa anthu onse, ndi momwe Iye akufuna kutambasula dzanja lake la chisomo kuti awapulumutse, kuwadalitsa, ndi kuwachiritsa. Mufunikanso kulangiza mamembala m'mene Mulungu akufunira kuwagwiritsira ntchito muutumiki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu, ndi momwe iwo eniwo angagwiritsire ntchito powonetsera mphatso zauzimu.

Chachiwiri, muyenera kukhala chitsanzo cha utumiki wopatsidwa mphamvu ndi Mzimu pamaso pa anthu. Njira yabwino yolimbikitsira mamembala kugwiritsa ntchito mphatso zauzimu ndikuwawonetsa momwe zimachitikira. Izi ndi zimene Yesu anachita ndi ophunzira ake. Anawasonyeza mmene angatumikire mu mphamvu ya Mzimu mwa kupulumutsa munthu wogwidwa ndi chiwanda (Luka 8:26-39) ndi kuchiritsa mkazi wodwala ndi kuukitsa mtsikana wakufa (vv. 40-56). Kenako “anawatuma kukalalikira ufumu wa Mulungu ndi kuchiritsa anthu odwala” (9:2). Choncho muyenera kulola kuti Mulungu akudzazeni ndikukudzazaninso ndi Mzimu Woyera. Kenako, muyenera kudalira Iye kuti adzakugwiritsani ntchito kusonyeza mphatso zauzimu pa moyo wanu ndi utumiki wanu.

Chachitatu, muyenera kulimbikitsa mamembala anu kukuyankhapo kuchitsogozo cha Mzimu Woyera ndikuchita mwachikhulupiriro kuti awonetsetse mphatso zauzimu. Muyeneranso kupereka mwayi kwa anthu kuti agwiritse ntchito mphatso panthawi ya kupembedza ndi kulalikira.

Pomaliza, muyenera kulimbikitsa mawonetseredwe a mphatso za uzimu mu mpingo poyesetsa kukulitsa mkhalidwe woyenerera mu mapemphero a mpingo. Mkhalidwe woterowo umadziwika ndi kupezeka kwa Mulungu ndi chikhulupiriro choyembekezera. Mulungu amaonetsera kupezeka Kwake pamene anthu Ake atsegula mitima yawo kwa Iye pomutamanda ndi kumulambira moona.

Chikhulupiriro choyembekezeka chimapangidwa pamene anthu a Mulungu akulimbikitsidwa kufikira ndi kuyembekezera kuti Mulungu awonetsere kukhalapo Kwake "ndi zizindikiro, ndi zozizwitsa ndi mphamvu zamitundumitundu ndi zogawira za Mzimu Woyera, monga mwa chifuniro chake" (Aheb. 2: 4).

Mbusa weniweni wa Chipentekoste adzayesetsa kukhala mwamuna kapena mkazi wa Mzimu. Adzapanga cholinga chawo kuphunzira kutumikira mu mphamvu ya Mzimu Woyera ndi zizindikiro zowatsatira, ndipo adzaphunzitsa anthu awo kuchita zomwezo.

~ Mutu 22 ~

Kumenya Nkhondo za Uzimu

Yesu anamvetsa kuti Iye anali nawo mu kulimbana kwakukulu kwauzimu ndi Satana ndi magulu ake ankhondo. Nthawi ina anatulutsa chiwanda mwa munthu wakhungu ndi wosalankhula. Anthu anangoyang'ana modabwa pamene munthuyo anayamba kuona ndi kulankhula. Ena anafunsa kuti, "Uyu si Mwana wa Davide kodi?" Ena amanong'onezana kuti: "Uyu samatulutsa ziwanda koma ndi mphamvu yake ya Belezebulu, mkulu wa ziwanda" (Mat. 12:22-24).

Yesu anadziwa maganizo awo ndipo anawauza kuti: "Ufumu uliwonse wogawanika pa wokha sukhalira kupasuka, ndipo mzinda uliwonse kapena banja logawanika pa lokha silikhala." Kenako anawafotokozera zimene zinali zitangochitika kumene, kuti: "koma ngati Ine ndimatulutsa ziwanda ndi mphamvu ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu." Kenako anawonjezera kuti: "Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ake, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? Ndipo pamenepo adzafunkha za m'banja lake" (Mat. 12:25-29).

N'chimodzimodzinso masiku ano; ifenso tili m'nkhondo yaikulu ndi mphamvu za zoipa. Tisanayambe kumasula anthu ku ukapolo wa uchimo ndi Satana, tiyenera kumenya nawo nkhondo yauzimu. Choyamba tiyenera kumanga munthu wamphamvuyo. Kenako, tikhoza kulanda nyumba yake. Mutu uwu ukambirana za kufunika kwa mbusa wa Chipentekoste kukhala okhoza kutsutsa ndi kugonjetsa mizimu ya ziwanda.

KUMVETSA NKHONDO YA UZIMU

Yesu asanabwerere kumwamba, anasiya mpingo wake ndiKutumidwa Kwakukulu. Iye analamula otsatira ake kuti: "Mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu woyera, ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu" (Mat. 28:19). Buku la Machitidwe a Atumwi ndi nkhani ya mmene ophunzira oyambirira a Khristu anayamba kukwaniritsa ntchito yake mu mphamvu ya Mzimu Woyera.

Kutumidwa Kwakukulu kumeneku kukugwirabe ntchito mpaka pano, ndipo ntchitoyi idzagwirabe "mpaka chimaliziro cha nthawi ya pansi pano" (v. 20). Kuti ntchito imeneyi igwirike bwino, mpingo ndi utsogoleri wake uyenera kudziwa momwe ungathanirane ndi Satana ndi ziwanda zake.

Zenizeni za Nkhondo Yauzimu

Nkhondo yauzimu ndi yeniyeni. Pali mdani weniweni, ndipo pali nkhondo zenizeni zauzimu zomwe ife monga abusa a Chipentekoste tiyenera kumenyana ndi kupambana. M'kalata yake yopita kwa Aefeso, Paulo ananena za nkhondo yauzimu imeneyi:

"Chifukwa kuti kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akuchita zolimbika a dziko lapansi amdima uno, ndi auzimu a choipa m'zakumwamba" (Aefeso. 6:12).

Mtumwiyu anafotokozanso mmene atumiki a Khristu apatsidwa zida zauzimu zamphamvu zoti azigwiritsa ntchito polimbana ndi zoipa: "pakuti zida zankhondo yathu sizili za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga" (2 Ako. 10:4)**.**

Anthu miyandamiyanda mu Afirika muno sanalandire umboni wokwanira wa uthenga wabwino. Anthu amenewa akukhala m'madera olamulidwa ndi zipembedzo zotsutsana ndi kufalikira kwa Chikhristu. Madongosolo amenewa amalamuliridwa ndi olamulira amphamvu a ziwanda, amenenso amalamuliridwa ndi Satana, "kalonga wa ziwanda" (Marko 3:22; fanizilani ndi 1 Yohane 5:19). Kuti apulumutse anthuwa, munthu wamphamvuyo ayenera kumangidwa ndi kuthamangitsidwa (Mat. 12:28-29). Choncho, ngati mpingo uyenera kukwaniritsa bwino ntchito ya Khristu, ukuyenera kuphunzira kuyenda mu mphamvu ya Mzimu

Woyera. Ndipo uyenera kudziwa momwe ungachitire ndikugonjetsa mphamvu za ziwanda.

Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera kuti: "Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga Kumwamba chomwecho pansi pano" (Mateyu. 6:10). Nthawi ina iye anawauza kuti: "Ndithu ndinena ndi inu kuti, Alipo ena akuimirira pano, amene sadzalawa imfa konse, kufikira akaona Ufumu wa Mulungu utadza ndi mphamvu" (Marko 9:1).

Yesu ankanena za Tsiku la Pentekoste, pamene ophunzira ake "adzavekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba" (Luka 24:49; Machitidwe 2:4).

Lero, ufumu wa Mulungu umabwera mu mphamvu nthawi iliyonse pamene wina wapulumutsidwa, kuchiritsidwa, kuwomboledwa, kapena kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mbusa wa Chipentekoste ayenera kutsogolera anthu ake kupemphera pafupipafupi kuti ufumu wa Mulungu udze mu mphamvu.

Mkhalidwe wa Nkhondo Yauzimu

Nkhondo yauzimu ndi mkangano pakati pa chabwino ndi choipa, pakati pa chimene chili choyera ndi chosayera. Mu nthawi ino, ndi kulimbana kosalekeza pakati pa Satana ndi ziwanda zake ndi Mpingo woona wa Mulungu.

Mdierekezi wasonkhanitsa chuma chake chonse kuti awononge ntchito yowombola ya Mulungu ya mafuko. Iye ndi wakupha ndi wabodza ndipo amafuna "kuba, kupha, ndi kuwononga" (Yohane 8:44; 10:10). Iye ndi ziwanda zake amagwira ntchito kuchititsa khungu maganizo a anthu kuti asazindikire choonadi cha uthenga wabwino (2 Akorinto 4:3-4). Chifukwa chakuti amadana ndi Mulungu, Mdierekezi amafuna kuti amugwetse ndi kumuvulaza. Komabe, akudziwa kuti sangampweteke Mulungu. Chotero iyeamafuna kusautsa ndi kuwononga awo amene Mulungu amawakonda, mtundu wa anthu.

Yesu analengeza kuti ufumu wa Mulungu wafika (Marko 1:14-15; Luka 8:1, 9:11). Iye analengeza molimba mtima kuti anadza kudzawononga ufumu wa Satana ndi kukhazikitsa ulamuliro wa Mulungu padziko lapansi. Uthenga wa ufumu wa Mulungu unalinso pamtima pa kulalikira kwa ophunzira a Khristu (fanizilani Machitidwe 8:12; 19:8). Yesu anawatuma kukalengeza ufumu wa

Mulungu ndi kusonyeza mphamvu zake pa "mphamvu zonse za mdaniyo" (Luka 10:19; onaninso Mateyu. 10:7; Luka 9:1-2; 10:8-9).[1]

KUKONZEKERA NKHONDO YA UZIMU

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kukhala okonzeka nthawi zonse kutsutsa ndikugonjetsa mizimu ya ziwanda. Ndipo inunso muyenera kuphunzitsa mamembala a mpingo wanu kuchita chimodzimodzi. Nazi njira zina zomwe mungakonzekere nkhondo yauzimu:

Dzazidwani ndi Mzimu Woyera

Choyamba, onetsetsani kuti mwadzazidwa ndi Mzimu Woyera (Mach. 2:4; 4:31) ndi kuti tsopano mukuyenda ndikukhala "moyenda ndi Mzimu" (Agal. 5:25). Yesu mwini anadzazidwa ndi Mzimu (Luka 3:21-22), ndipo anakhala ndi kutumikira mu mphamvu ya Mzimu (Luka 4:18-19; Mach. 10:38). Yesu anachitira umboni kuti ndi mphamvu ya Mzimu Woyera anatulutsa ziwanda (Mat. 12:28). Ngati tingathe kuchita bwino pankhondo ya uzimu, ifenso tiyenera kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera.

Zindikirani Zimene Khristu Anachita

Kenako, pokonzekera nkhondo yauzimu, muyenera kuzindikira zonse zomwe Khristu adakwaniritsa pa Kalvare. Kumeneko, analipira mtengo wa chiombolo cha anthu (Yeseya. 53:6; 1 Yohane. 2:2). Anawononganso ulamuliro wa mdierekezi pa dziko lapansi (Yohane 12:31). Baibulo limatiuza kuti Khristu "atavula maukulu ndi maulamuliro, anawaonetsera poyera, nawagonjetsera nako" (Akolose. 2:15)**.**

Tsopano, chifukwa cha ntchito yamphamvu ya Khristu pa Kalvare, Satana ndi ziwanda zake ali adani ogonjetsedwa (Ahebri 2:14-15). Ngati tiyenda mu Mzimu, ndi kudzipereka tokha kwathunthu kwa Khristu ndi chifuniro **c**hake, Iye adzatipatsa ife mphamvu ndi ulamuliro umene tikufunikira kuti tigonjetse Satana ndi ziwanda zake.

---

[1] Kuti mudziwe zambiri za Ufumu wa Mulungu omwe uli nkudza, onani buku la Chiyembekezo cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Ufumu wa Mulungu: Kutanthauzira mwa Chipentekoste* lolembedwa ndi Denzil R. Miller, *lofalitsidwa* ndi Africa Theological Training Service (https://africaatts.org/).

Kumbukirani Chomwe Muli mwa Khristu

Kuonjezera apo, pokonzekera nkhondo yauzimu, muyenera kudzikumbutsa nokha kuti ndinu ndani mwa Khristu. Ngakhale mukukhala pano padziko lapansi, monga mwana wa Mulungu, ndinu nzika ya kumwamba (Afilipi 3:20). Ngati mungakumbukire chowonadi ichi, ndikusankha kukhala ngati mwana weniweni wakumwamba, Yehova adzakupatsani zonse, ulamuliro, ndi mphamvu za dzikolo. Pamene muphunzira kuganiza ndi kuchita monga nzika ya ufumu wa Mulungu, m'pamenenso mudzakhala okonzeka kwambiri kulengeza uthenga wabwino wa ufumu kwa anthu otayika, ndipo m'pamenenso mudzakhala wokhoza kumenya nkhondo m'malo auzimu.

Valani Zida Zonse za Mulungu

Pomaliza, Paulo akulimbikitsa ankhondo auzimu kuti "tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimba kwa mphamvu yake" (Aefeso. 6:10). Njira imodzi imene tingachitire zimenezi ndiyo kuvala zida zonse za Mulungu. Kenako, tsiku loipa likadzafika,tidzatha kuima nji polimbana ndi mdani (vv. 11, 13).

Kenako Paulo anatchula zida zisanu ndi ziwiri zamphamvu zauzimu zomwe Khristu wapereka kwa atumiki ake. Amaperekanso zidziwitso za momwe chida chilichonse chingagwiritsire ntchito kumenya nkhondo yauzimu (Aef. 6:13-18). Tiyeni tiwone bwinobwino zida zisanu ndi ziwiri zauzimu izi:

1. *Lamba wa choonadi*. Choyamba, tiyenera kudzimanga ndi "lamba wa choonadi" (Aef. 6:14). Kuvala lamba wa choonadi kumatanthauza zinthu ziwiri: Kumatanthauza kuti tidzikonzekeretsa ndi choonadi cha Mawu a Mulungu (Yoh. 17:17). Kumatanthauzanso kuti tiyenera kudzikulunga m'choonadi, ndiko kuti, m'kuona mtima kotheratu ndi kukhulupirika. Ndi chida ichi tidzatha kutsutsa mabodza a mdierekezi (Yoh. 8:44).

2. *Chodzitetezera pachifuwa cha chilungamo*. Kenako, tiyenera kukonzekera nkhondo yauzimu mwa kuvala "chapachifuwa cha chilungamo" (Aef. 6:14) Timachita izi poonetsetsa kuti tili pa ubale wabwino ndi Mulungu, komanso kuti tikukhala mu chiyanjano chosasweka ndi Yesu Khristu (Yoh. 15:5). Chifukwa cha unansi umenewu, timatha kukhala ndi moyo waukhondo ndi woyera

3. *Mapazi okonzeka*. Chachitatu, tiyenera kudzikonzekeretsa tokha ndi "kukonzeka" (Aef. 6:15). Mwa kuyankhula kwina, tiyenera kukhala osamala nthawi zonse ndi mdani wathu (1 Petro. 5:8*).* Kukonzekera kumeneku

kumapangidwa ndi kumva ndi kumvera uthenga wabwino. Komanso, monga abusa okhulupirika a gulu la nkhosa la Mulungu, tiyenera kukonzekeletsa anthu a Mulungu kaamba ka kuukira kwa adani, monga momwe Paulo anachitira ndi akulu a ku Aefeso (Mac. 20:28-31).

4. *Chishango cha chikhulupiriro*. Chachinayi, tiyenera kunyamula "chishango cha chikhulupiriro" (Aef. 6:16). Tikhoza kugwiritsa ntchito chida chauzimu chimenechi ngati chitetezo ku "mivi yonse yoyaka moto ya woipayo" (v. 16). Mivi yoyaka moto imeneyi imaphatikizapo mayesero osiyanasiyana a mdierekezi monga maganizo oipa ndi zilakolako ndi zonyengerera kuti tisamvere malamulo a Mulungu. Chikhulupiriro chathu chimamangika pakumvetsera ndi kuwerenga Mawu a Mulungu (Aroma 10:17) ndi kupemphera mu Mzimu Woyera (Yuda 20).

5. *Chisoti cha chipulumutso*. Chida chachisanu chomwe tili nacho ndi "chisoti cha chipulumutso" (Aef. 6:17). Chipulumutso chimenechi chimaphatikizapo, osati kupulumutsidwa kokha ku uchimo ndi gahena, komanso chipulumutso chilichonse kapena chiwombolo chilichonse chochokera kwa Mulungu, monga kupulumutsidwa ku ziwanda, ngozi, matenda, ndi imfa.

6. Mawu a Mulungu. Chachisanu ndi chimodzi, tiyenera kutenga "lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu" (Aef. 6:17). Mawu a Mulungu ndi chimodzi mwa zida zauzimu za mbusa wa Chipentekoste. Tikhoza kudzikonzekeretsa tokha ndi Mawu a Mulungu mwa kuphunzira mwakhama ndi kuloweza malemba (Masalmo 119:11). Komanso, tiyenera kulengeza Mawu a Mulungu mokhulupirika kwa onse amene angamvetsere (2 Tim. 4:2).[2]

Mawu a Mulungu atha kugwiritsidwa ntchito pankhondo yopita chitsogolo (makani) komanso yodzitchinjiriza. Itha kugwiritsidwa ntchito ngati chida chopitira chitsogolo mwa makani pamene Mawu agwiritsidwa ntchito m'pemphero, komanso pamene alalikidwa ndi kuphunzitsidwa pansi pa kudzoza kwa Mzimu. Ndipo angagwiritsidwe ntchito ngati chida chodzitetezera polimbana ndi kuukira kwa Satana, monga momwe Yesu anachitira m'chipululu (Luka 4:1-13).

[2] Kuti mudziwe zambiri zokhudza ubale wa Mbusa wa Chipentekoste ndi Baibulo, onani Mutu 9: "Amakhulupirira Baibulo."

"Mawu a Mulungu" otchulidwa m'ndime iyi atha kukhalanso mawu aumwini kapena a *rhema* amene wophunzira wa Khristuangalandire kuchokera kwa Mzimu. Imeneyi ikhoza kukhala ndime ya m'Baibulo imene Yehova amaika pa mtima wa munthu. Kapena likhoza kukhala vumbulutso lochokera kwa Mulungu kuti likwaniritse chosowa chapadera, monga mawu achidziwitso kapena mawu anzeru (1 Akorinto 12:8).

7. *Pemphero mu Mzimu.* Pomaliza, tiyenera kutenga chida cha pemphero mu Mzimu. Pemphero loterolo ndi chida champhamvu chauzimu. Motero Paulo akulimbikitsa okhulupirira "mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu" (Aef. 6:18). Izi zikutanthauza kuti nthawi zambiri tiyenera kulola Mzimu Woyera kutidzoza ndikuwongolera mapemphero athu. Kupemphera kwamtunduwu kumaphatikizapo kupemphera m'malilime (1 Akorinto 14:14; onaninso Aroma 8:26).

Zida Zina Zisanu ndi Ziwiri Zauzimu

Baibulo limakamba za zida zisanu ndi ziwiri zamphamvu zauzimu zomwe mbusa wa Chipentekoste angagwiritse ntchito kuti agonjetse mdani:

1. *Chida chosala kudya*. Kugwiritsidwa ntchito kusala kudya pamodzi ndi pemphero, kusala kudya ndi chida champhamvu chauzimu (Marko 9:29).

2. *Chida choyamika*. Mphamvu yayikulu yauzimu imapangidwa kudzera mu matamando odzozedwa ndi Mzimu. Pamene anthu a Mulungu atamanda, malinga amagwa (Yoswa 6:16-20), magulu ankhondo akugonjetsedwa, (2 Mbiri 20:1-26) ndipo zitseko za ndende zinatsegulidwa (Mach. 16:25-26).

3. *Chida cha chikondi*. Chikondi chenicheni chili ndi mphamvu yodabwitsa potsogolera amuna ndi akazi kwa Khristu (Aroma 5:5). Ena, amene sitingapambane ndi kuwakopa mwa malankhulidwe, kapena kuwonetsera mphamvu zathu, tikhoza kupindula kwa Khristu kudzera mu mawonetseredwe osavuta a chikondi chachikhristu (12:20-21).

4. *Chida cha ubatizo wa Mzimu Woyera*. Yesu analonjeza otsatira ake mphamvu pamene Mzimu Woyera anadza pa iwo (Mach. 1:8). Amalankhula za ubatizo wa Mzimu Woyera (Luka 3:16; Machitidwe 1:5; 2:4).[3]

[3] Kuti mudziwe zambiri zokhudza ubatizo wa Mzimu Woyera, onani Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

5. *Zida za mphatso za Mzimu.* Chifukwa chimodzi chimene Mzimu amapereka mphatso zake ku mpingo ndi chakuti okhulupirira akhale okonzeka kumenya nkhondo ya uzimu (1 Akorinto 12:8-10).[4]

6. *Chida cha dzina la Yesu*. Ulamuliro wonse wakumwamba waima kumbuyo kwa dzina la Yesu (Afilipi 2:9-11). Pamene tigwiritsa ntchito dzina lake monga momwe adalamulira, mphamvu za gahena ziyenera kudzipereka (Yohane 14:13-14; Machitidwe 3:6; 9:27; 16:18).

7. *Chida cha uthenga wabwino.* Paulo anatcha Uthenga Wabwino kuti "mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa yense wakukhulupirira" (Aroma 1:16). Uthenga Wabwino ndi uthenga wa chipulumutso mwa Khristu. Uthenga Wabwino uli ndi mphamvu yakulenga chikhulupiriro m'mitima ya anthu amene amaumva ukulalikidwa (Aroma 10:17). Sitiyenera kulephera kulalikira uthenga wabwino mokhulupirika nthawi iliyonse (1 Akorinto 9:16).

KUCHITA NKHONDO YA UZIMU

Funso nali, "Kodi Mbusa wa Chipentekoste (kapena, kwenikweni, wophunzira aliyense wodzazidwa ndi Mzimu)angayang'anizane ndi kutulutsa mizimu yoipa mwa munthu wogwidwa ndi ziwanda? Nazi njira zitatu zomwe mungagwiritse ntchito potumikira chiwombolo kwa iwo omwe ali mu ukapolo wa ziwanda.[5]

[4] Onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

[5] Pa zambiri zokhudza kutsutsa ndi kugonjetsa mizimu ya ziwanda, onani buku la Chiyembekezo cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Utumiki Wamphamvu*, Mutu 11: "Momwe Mungatulutsire Ziwanda" ndi Mutu 12: "Kugonjetsa Mizimu Yachigawo."

Funsani mafunso

Gawo loyamba potumikira mamasulidwe kwa ogwidwa ndi ziwinda ndi kufunsa mafunso, ngati izi zingatheke. Munthawi imeneyi, mudzalankhula ndi munthu amene akufunika kupulumutsidwa. Cholinga chanu ndi kudziwa zambiri za makhalidwe a munthuyo. Panthawi imeneyi, kudzera mu mphatso ya kuzindikira mizimu,mutha kuzindikira kupezeka kwa ziwanda. Kapena ziwanda zingavutike ndi kukhalapo kwa Mulungu ndi kudziulura zokha (Marko 1:23; 5:6-7). Ngati n'kotheka, mutsogolere wogwida ndiziwandayo m'pemphero la kulapa ndi kuulula machimo.

Izi nzofunika makamaka pamene machimo a munthuyo ali ogwirizana kwambiri ndi ukapolo wake wauzimu. M'pempherolimeneli, womasulidwayo ayenera kulengeza za kuleka khalidwe lokopa ziwanda ndi ntchito zotsatizana nazo za thupi m'moyo wake.

Kuchita Utumiki

Gawo lachiwiri la njira yopulumutsira ndi kuchitapo kanthu kwa utumiki. Uku ndiko kukumana ndi mphamvu zenizeni ndi mphamvu za ziwanda. Choyenera kuchita poyamba ndi kuyitanira pa dzina la Yesu ndikuitana Mzimu Woyera kuti abwere ndikuwonetsa kupezeka kwake ndi mphamvu zake. Mukangozindikira kukhalapo kwa Mulungu, mutha kupitiriza kutulutsa (kapena nthawi zina, kuthamangitsa) ziwanda. Pamene Mzimu amatsogolera, mutha kugwiritsa ntchito imodzi kapena zingapo mwa njira za m'Baibulo izi:

- Mukhoza kumanga ziwanda m'dzina la Yesu (Mat. 16:17-19; 18:18).
- Mukhoza kulamula ziwandazo kuti zituluke, zichoke, kapena kuti zimasule munthu amene wagwidwa nazo (Luka 4:35).
- Mukhoza kulamula ziwanda kuti zisalowenso mwamunthuyo (Marko 9:25).

Nthawi zina ziwanda zimakana kutuluka, ndipo padzakhala kulimbana (Luka 8:29; 11:14). Zikatero, muyenera kulimbikira m'chikhulupiriro mpaka kupambana kutafika. Kupulumutsidwa nthawi zambiri kumatsagana ndi mawonetseredwe a thupi (Marko 7:30; Luka 4:33-35; 9:42). Izi zikachitika, musamachite mantha kapena kudodometsedwa. M'malo mwake, muyenera kupitiriza kuyenda mu mphamvu ya Mzimu Woyera, kulamula kuti ziwandazo zikhale chete (Marko 1:25), ndipo mu ulamuliro wa dzina la Yesu, muzilamula kuti zituluke ndi kukhala kunja (Marko 9:25)

Uphungu Pambuyo pa Pemphero

Gawo lomaliza la njira yopulumutsira ndi uphungu wa pambuyo pa pemphero. Njira imeneyi ndi yofunika kwambiri kwa munthu amene wakhala akulamulidwa ndi ziwanda. Adzafunikira pemphero ndi chochirikiza chamalingaliro pambuyo pa kuwomboledwa kwawo. Ngati munthuyo sanabadwe mwatsopano, muyenera kumutsogolera nthawi yomweyo ku chikhulupiriro mwa Khristu. Kuonjezera apo, muwatsogolere nthawi yomweyo mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Yesu anachenjeza za kunyalanyaza zinthu zofunika zimenezi (Mat. 12:43-45). Inu, kapena wina amene mwamtuma, muyenera kukhala pafupi kwambiri ndi munthuyo mpaka atamasulidwa ku ukapolo wake.

Monga Mbusa wa Chipentekoste, Khristu wakutumani kuti muchite nkhondo yauzimu (Marko 16:15-16). Mungathe kulimbana ndi mdierekezi ndi ziwanda zake molimba mtima, podziwa kuti Iye amene amakhala mkati mwanu ndi wamkulu kuposa iye amene ali m'dziko lapansi (1 Yohane 4:4).

~ Gawo 6 ~

MBUSA WA CHIPENTEKOSTE NGATI OWETA NKHOSA

~ Mutu 23 ~

Kumvetsetsa Utumiki wa Mbusa

Ndizotheka ndithu kuti munthu kukhala wotenga nawo mbali mu zinthu za chipembedzo, ndikudzipereka kwathunthu kuzochitikazo, koma nthawi yomweyo osamvetsetsa bwino zomwe akuchita kapena chifukwa chimene akuchitira zinthu. Mzimu Woyera anatsogolerapo Filipo kwa mdindo wolemekezeka, woona mtima ndi wodzipereka wa ku Etiopiya. Wolemekezekayu anali kuwerenga Malemba. Komabe, iye sadamvetsetse zomwe amawerenga (Mach. 8:29-31). Mu nthawi ina, Paulo anakumana ndi amuna oona mtima odzipereka a ku Aatene. Anthuwa amalambira kwa "MULUNGU WOSADZIWIKA." Komabe, sadamvetsetse amene iwoamamulambira kapena chifukwa chake (Mach. 17:22-23). Amafunikira kufotokozeredwa.

Abusa ambiri a Chipentekoste mu Afirika amadzipezekeretsa okha munyengo zonga izi. Iwo amakhala ochitachita mu utumiki wa ubusa, ndipo ndi odzipereka mwakuya mukukwaniritsa udindo wao ngati Mbusa. Komabe, m'choonadi, amamvetsetsa zochepa za zomwe akuchita kapena chifukwa chimene akuchitira izo. Monga mdindo wolemekezeka wa ku Etiopiya, amadandaulira, "Ndingathe bwanji, popanda munthu wonditsogolera?" izi zalembedwa kuti ziyankhe kudandaulaku. Izi zikuyala maziko akamvetsetsedwe ka utumuki wa abusa, maziko amene utumuki wolimba ungamangidwepo.

MALO A UTUMIKI WA UBUSA

Utumiki wa ubusa umachitika mu mpingo wa pamalo. Mau a chigiriki okhudza mpingo mu Chipangano Chatsopano ndi *ekelezia,* amene amatanthauza iwo amene ayitanidwa ndi kupatulidwa. Choncho, mpingo wa pamalo ndi gulu la anthu omwe apatulidwa mwa Khristu kuti atumikire ndi kulambira Iye. Umapangidwa ndi iwo amene abadwa mwa Mzimu wa Mulungu ndi kutsukidwa mu mwazi wake (Yoh. 3:3-7; Mach. 20:28).

Zinthu zitatu zitha kunenedwa zokhudza mpingo: choyamba, mpingo ndi wake wa Mulungu. Yesu adatcha mpingo kuti "Mpingo wanga" (Mateyu 16:18). Paulo adawutcha kuti "Nyumba ya Mulungu….Ekelezia wa Mulungu wa moyo" (1 Tim. 3:15). Chachiwiri, mpingo ndi malo okhalilamo. Paulo akuyakhula za mpingo kuti ndi "Kachisi oyera" amene "wakhala chokhalamo Mulungu mwa Mzimu" (Aefeso 2:22). Chotsiriza, mpingo ndi "mzati ndi mchirikizo wa choonadi" (1 Tim. 3:15). M'mau ena, ndi chimango cha uzimu chomwe chimanthandizira ndi kusunga choonadi. Chimodzi mwa nntchito ya mpingo ndi kusunga ndi kulengeza choonadi (Mat. 28:19; 2 Ako. 2:14). Ngati Mbusa wa chipentekoste, uyenera kukhala odziwa ndithu kuti uchite utumiki wako mmaonedwe amenewa.

LINGALIRO LA UTUMIKI

Ndizofunikiranso kwambiri kuti umvetsetse lingaliro la Baibulo pa utumiki. Malemba amaphunzitsa kuti Khristu anasankha mautumiki mu Mpingo kuti athe kupangitsa iwo kukwaniritsa chake choperekedwa ndi Mulungu. Cholinga cha Mulungu ku mpingo ndi kuti ulalikire uthenga wabwino kwa anthu onse mu mphamvu ya Mzimu Woyera kubweranso kwa Khristu kusanachitike (Marko 16:15-16; Mach. 1:8). Kenako, muyenera kutenga okhulupirira ndikuwapanga iwo kukhala ophunzira omvera, kuwaumba iwo mu chifanizo cha Mbuye wao (Mat. 28:19; Akolose 3:10).

Liwu lakuti *utumiki* limanyamulanso koposa malingaliro a nntchito ndi kachitidwe. Paulo akufotokozera lingaliro la utumiki. Mu Aefeso 4, akuyankhula za mitundu inayi ya utumiki:

Utumuki wa Yesu

Choyamba, Paulo akuyankhula za utumiki wa Yesu, Mesiya (Aef. 4:8-10). Kudzera mu ntchito Yake yakuombola pamtanda (kuphatikizapo imfa Yake, kuikidwa mmanda, kuuka, ndi kukwera kwake kwa Atate), Yesu adakhazikitsa Chipangano Chatsopano. Ali pa dziko lapansi Khristu adatumikira ngati mtumwi (Ahebri 3:1), mneneri (Luka 24:19), mlaliki (Luka 19:10), Mbusa (Yohane 10:11-16), komanso mphunzitsi (Yohane 3:2; 13:13). Motero Iye adakhala "mwala wa pangodya" wa mpingo, kuonetsetsa kukhazikika ndi kupitirira kwake (Aef. 2:20).

Utumiki wa Okhulupirira

Chachiwiri, Paulo akuyankhula za utumiki wa okhulupirira (Aef. 4:11-16). Yesu anadalira utumiki wake ku Mpingo. Choncho, utumiki wina uliwonse mu mpingo ndi chikulitso cha utumiki wake. Cholinga cha utumiki ndi kuti membala aliyense pa mpingo akhale okhwima "Ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu" (Aef. 4:13). Iwo amene akhala okhwima ayenera tsopano kutembenuka ndi kulimbitsa ena, kupangitsa mpingo onse kuti ukule ndi kupambana.

Mautumiki a Utsogoleri

Chachitatu, Paulo akukamba ma utumiki a utsogoleri amene Christu anapereka ku Mpingo. Iye akulemba, "Ndipo Iye (Khristu) anapatsa ena akhale atumwi, ndi ena aneneri, ndi ena alaliki, ndi ena abusa, ndi ena aphunzitsi" (Aef. 4:11). Ma udindo a utumiki otere asamaonedwe chabe koyamba ngati mpando kapena udindo monga ambiri achitira. koma aganiziridwe kuti ndi ntchito yoyenera kugwiridwa ya utumiki. Si maudindo omwe atsogoleri amalamulira pa mpingo. Koma, ndi ntchito zomwe zaperekedwa kwa atsogoleri otumikira kuti "akonzere oyera mtima ku ntchito ya utumiki (Aef. 4:12), monga zotsatilazi:

- *Ntchito ya Utumwi:* Mtumwi amatumikira mpingo ndi zolinga za Mulungu pakupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu m'madera osafikilidwa komanso pakati pa anthu omwe sanafikiridwe mu mphmvu ya Mzimu Woyera—ndi kuphunzitsa ena kuchita zomwezo.
- *Ntchito ya Uneneri:* Mneneri amatumikira Mpingo ndi zolinga za Mulungu pakuyankhula uthenga wochokera kwa Mulungu mu mphamvu ya Mzimu Woyera—ndi kuphunzitsa ena kuchita zomwezo.
- *Ntchito ya Alaliki:* Mlaliki amatumikira Mpingo ndi zolinga za Mulungu pakulengeza uthenga wabwino kwa otayika mu mphamvu ya Mzimu Woyera—ndi kuphunzitsa ena kuchita zomwezo.

- *Ntchito ya Ubusa:* Mbusa amatumikira Mpingo ndi zolinga za Mulungu pakutumikira kwa anthu a Mulungu mu mphamvu ya Mzimu Woyera—ndi kuphunzitsa ena kuchita zomwezo.
- *Ntchito ya Uphunzitsi:* Mphunzitsi amatumikira Mpingo ndi zolinga za Mulungu pakuphunzitsa Mau a Mulungu mu mphamvu ya Mzimu Woyera—ndi kuphunzitsa ena kuchita zomwezo.

Ntchito za utumikizi nthawi zambiri zimalowana, ndi anthu ena kugwira ntchito mmaudindo ambiri. Mwachitsanzo, munthu atha kugwira ntchito ngati ndi mneneri pa nthawi yomweyo. Wina atha kugwira ntchito ngati mphunzitsi ndi mlaliki, ndikumatero. Monga zanenedwa mwambamu, Yesu anagwira ntchito mu zisanu zonse za ntchitozi, monga anachitira mtumwi Paulo. Mukulemba kwake pa ndime 11, Paulo akuoneka kuti akuphatikiza ntchito za Mbusa ndi mphunzitsi kukhala ntchito imodzi ya Mbusa-mphunzitsi.

Mkatikati mwa kachitidweka, Paulo akudzionetsera yekha ngati "Kapolo wa Yesu Khristu, mtumwi woitanidwa" (Arom. 1:1; fanizilani Tito 1:1). Chomwecho, Petro akudzionetsera yekha ngati "Kapolo ndi mtumwi wa Yesu Khristu" (2 Pet. 1:1). Onani mmene onse awiri akulengeza koyamba kuti ndi akapolo. Pokhapokhapo ndi mmene iwo akhale atumwi enieni. Zikhale chomwecho lero kwa wina aliyense amene akutumikira mu utumiki ulionse wautsogoleri. Pamwamba pa zonse ayenera kudziona iwo eni kuti ndi akapolo a Mulungu ndi anthu Ake (fanizilani Yohane 21:15-17; 1 Pet. 5:2-4).

Izi mphatso zisanu za Khristu "m'mene anakwera kumwamba" koposa zimatumikira ngati chionetsero cha ulamuliro wa Khristu mkatikati mwa Mpingo. Zolinga zao ndikutsogolera Mpingo mukulunjika ku zolinga zake za umulungu. Paulo adaphunzitsa kuti mautumiki amenewa ali ndi magawo awiri, kudzala ndi kuthirira. (1 Ako. 3:6). Mautumiki akudzala atha kuphatikizapo atumwi ndi alaliki. Mautumuki akuthirira atha kuphatikizapo aneneri, abusa, ndi aphunzitsi. Kugwira ntchito limodzi pakati pa odzala ndi othirira umapititsa ntchito ya Mulungu patsogolo.

Mautumiki ena Akutumikira

Motsatirana ndi mautumiki a atsogoleri, Mulungu waikiza mautumiki a ntchito zina mu Mpingo. Mautumiki amenewa akuphatikizapo, akulu a mpingo, madikoni amuna ndi akazi (fanizila Machitidwe 6:1-6; 14:23; 1 Tim. 3:1-10).

Liwu la Chihebri lokhudza 'mkulu' ndi *zaqen*, lomwe likusonyeza munthu wodziwa ndi wa ulamuliro (Numeri 11:16). Liwu la Chigiriki lokhudza 'mkulu' ndi *presbyteros*, lomwe limatanthauza mochuluka chimodzimodzi. Wankulu mu mpingo ndi amene ali ndi ulamuliro wakutumikira ngati oyang'anira (*episkopos* mu chigiriki) (Mach. 20:17, 28). Choncho, Mbusa ali zonse ngati wankulu komanso woyang'anira (Mach. 20:17, 28; 1 Tim. 3:1-2; Tito 1:5-7). Kuti atsogolere bwino lomwe mpingo, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kukhala okhwima mu uzimu, komanso iye akhale ndi chidziwitso chokwanira cha Mau a Mulungu (1 Tim. 3:6; 2 Tim. 4:2).

Liwu la Chigiriki lokhudza dikoni ndi *diakonos,* lomwe limatanthauza "amene amatumikira." Mu Machitidwe 6, amuna asanu ndi awiri odzala ndi Mzimu adasankhidwa kuti atumikire pamagome azakudya kuti pamenepo atumwi atha "kulimbika m'kupemphera ndi kutumikira mau" (Mach. 6:2-4). Awiri mwa amunawa Stefano ndi Filipo, anakhala mboni za mphamvu za Khristu. Mu Aroma 16:1, Paulo akuonetsera Febe ngati dikoni wa mkazi ku mpingo wa ku Roma.

NTCHITO YA MBUSA

Liwu la Baibulo lonena za Mbusa" limachokera ku liwu la chigiriki *poimēn,* omwe amatanthauza "Woyang'anira." Monga Mbusa, ntchito yako ndi kuyang'anira khosa za Mulungu (Machitidwe 20:28).. Ngati woyang'anira uyenera kutumikira ngati tsogoleri, phunzitsi, komanso oteteza anthu a Mulungu (1 Pet. 5:1-4).

Maudindo a Mbusa

Pamndanda wa maudindo ako ngati Mbusa ndi kusamalira nkhosa (Yohane 21:15-17; 1 Pet. 5:2-3), kulimbitsa thupi (Aef. 4:11-12), kupereka uphungu kwa anthu a Mulungu (1 Tim. 5:14), kuteteza nkhosa (Mach. 20:28). Maudindo ena akuphatikizapo kulalikira (2 Tim. 4:2), kuphunzitsa (1 Tim. 3:2; Tito 2:1), kutsogolera (Ahebri 13:17), kasamalidwe (Machitidwe 20:28), kupanga-ophunzira (Mat. 28:19), kulalikira kwa otaika (2 Tim. 4:5), ndi kubweretsa pamodzi mpingo ku utumwi (Mach. 13:1-4).[1]

M'masiku oyambirira a mpingo, Tsiku la Pentekoste litangodutsa, atumwi anayambiratu udindo wa ubusa. Anatsogolera mpingo m'mene Khristu

[1] Pa zambiri zokhudza udindo wa Mbusa wa Chipentekoste, onani mitu 23-27.

adawatsogolera iwo, kutsindika za zomwe Iye anatsindika. Zochuluka za zomwe iwo anatsindika zavumbulutsidwa mu zolemba za Luka zokhudza mpingo mu Machitidwe 2:38-47.

Ndime imeneyi limodzi ndi ndime zina zotsatira zake,zikuonetsera zotsindika khumi zokhudza ubusa wa atumwi. Ngati Mbusa wa Chipentekoste, utha kukhala wa nzeru pakutsatira chitsanzo cha atumwi, kulora zinthu khumi izi kuti zipereke maonedwe a utumiki wanu lero lino.

1. Kulengeza uthenga wabwino. Mwatsopano atapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera, Petro adaima ndi kulengeza molimba mtima uthenga wabwino. Mu ulaliki wake pa Tsiku la Pentekoste, Petro anatsindika za imfa ndi kuukanso kwa Khristu (Machitidwe 2:23-24, 32; fanizila 1 Ako. 15:1-4). Adamaliza uthenga wake pakuyitanira anthu onse kukulapa ndi kukhulupirira uthenga wabwino (Machitidwe 2:36-40). Kutsindika uku kunapitirira (Machitidwe 3:19; 20:21; 26:20). Munjira yomweyo, kulengeza kwa uthenga wabwino kukhale phata la utumiki wanu wa ubusa tsiku la lero.[2]

2. Kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Petro anatsindikanso zakufunikira kwa kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera (Mach. 2:38-39; fanizilani 2:17-18). Iwo amene alandira Khristu apatsidwe mwawi nthawi yomweyo yakudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Monga kulengeza kwa uthenga wabwino, chotsindika ichi chinapitilira mu Machitidwe monse (8:14-17; 9:17-18; 10:44-46; 19:1-7). Ngati Mbusa wa Chipentekoste mu Afirika, muyenera kuchita chimodzimodzi. Muyenera kulalikira ndi kuphunzitsa nthawi zambiri za ubatizo mu Mzimu Woyera ndi cholinga choti muone membala aliyense akupatsidwa mphamvu mukuchitira umboni kwa ena otayika. (1:8).[3]

3. Kuphunzitsa Mau a Mulungu. Koposa, Luka akutiuza kuti okhulupirira a ku Yerusalemu "anali chikhalire m'chiphunzitso cha atumwi" (Mach. 2:42). Atumwi motero adatsindika za kuphunzitsa Mau a Mulungu. Patadutsa zaka, Paulo adachitira umboni, "sindinakubisirani zinthu zopindulira, osazilalikira kwa inu, ndi kukuphunzitsani inu pa bwalo ndi m'nyumba zanu" (20:20). Aka kadali kachitidwe ka Paulo kulikonse amapita (fanizilani 11:26-26; 15:35; 28:31). Inunso

[2] Pa zambiri zokhudza utumiki wakulalikira wa Mbusa wa Chipentekoste, onani mutu 16: "Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu."

[3] Pa zambiri zokhudza kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera onani mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira ku Ubatizo wa Mzimu Woyera."

onetsetsani kuti Mau a Mulungu akuphunzitsidwa ponseponse, molondola, komanso momveka bwino mu mpingo omwe Mulungu wakuitanirani kuti mutsogolere.[4]

4. Kukondwerera ma Sakramenti. Mu kumvera zolamulira za Yesu (Mat. 28:19-20; Luka 22:19), atumwi anatsindika ubatizo wa madzi ndi Mgonero (Mach. 2:38-41). Ubatizo wa madzi umachitira umboni za kubadwa mwatsopano kwa okhulupirira. Mgonero umachitira umboni ku chiyanjano chomwe chikupitilira ndi Khritsu. Monga Mbusa wa Chipentekoste uwonetsetse kuti miyambo yopatulikayi ikuchitika mokhulupirika mu mpingo.[5]

5. Kutsongolera M'mapemphero. Atumwi koposanso anatsindika za pemphero. Luka, akutiuza kuti anthuwa "Adadzipereka okha…ku pemphero" (Machitidwe 2:42). Pemphero lodzipereka limaumba maziko a kudzimvera chisoni ndi kuchitira umboni kwa okhulupirira. (fanizilani 4:31). Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutsogolera anthu m'mapemphero kudzera muchiphunzitso ndi za iwe mwini.[6]

6. Kuyembekezera zizindikiro ndi zodabwitsa. Atumwi adapitiriranso kufunitsitsa chionetsero cha kupezeka kwa Mulungu ndi mphamvu mu mpingo. Luka akulemba, "Koma panadza mantha pa anthu onse, ndipo zozizwa ndi zizindikiro zambiri zinachitika ndi atumwi" (Mach. 2:43). Kuonetsera kwa kupezeka kwa Mulungu ndi mphamvu Yake chikhale chikhalidwe cha utumiki wanu ngati mbusa wa Chipentekoste lero.[7]

7. *Kukweza Umodzi.* Komanso, atumwi amakweza umodzi mu thupi. Luka akulemba, "Ndipo onse akukhulupirira anali pamodzi, nakhala nazo zonse zodyerana" (Mach. 2:44). Umodzi wa anthu ukuyankhulidwa apa, unali oposa ku thupi. Adali ndi umodzi wa pa mtima ndi cholinga chomwe chinapititsa patsogolo mpingo ku ntchito yake.

---

[4] Pa zambiri zokhudza utumiki wakuphunzitsa wa Mbusa wa Chipentekosite, onani mutu 17: "Kuphunzitsa kwa bwino."

[5] Pa zambiri zokhudza kaperekedwe ka Masakramenti, onani Mutu 42: "Kuchititsa ma Sakramenti, Kupereka, ndi Kukhazikitsa."

[6] Pa zambiri zokhudza Mbusa wa Chipentekosite ndi Pemphero, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

[7]Pa zambiri zokhudza utumiki mu zauzimu, onani Mutu 21: "Kutumikira mu Mphamvu ya Mzimu."

8. Kulimbikitsa Kupereka. Kuphatikiza apo, atumwi adakweza mchitidwe wakupereka. Zotsatira zake, mamembala a mpingo "Anagulitsa chuma chao, nazigawira kwa onse, monga momwe yense anasowera" (Mach. 2:45). Kusaumira kotere kunabadwa kuchokera pa ubwenzi wa kukondana wina ndi mzache komanso ndi Mbuye wao. Ngati atumwi, inunso muyenera kutsogolera anthu anu mukupereka mosaumira ku ntchito yake ya Mulungu.

9. Kukonza Mapemphero. Luka akulemba, "Ndipo tsiku ndi tsiku anali chikhalire ndi mtima umodzi m'kachisi….nalemekeza Mulungu, ndi kukhala nacho chisomo ndi anthu onse" (Mach. 2:46-47). Atumwi anadziwa kufunikira kwake kwa kudza pamodzi kwa anthu kudzalambira, kuphunzitsidwa, ndi kulimbikitsana.[8]

10. Kubwera pamodzi m'kuchitira umboni. Chotsiriza, atumwi adatsindika kuchitira umboni kwa aliyense payekha. Anasonkhanitsa anthu pamodzi, kuwalimbikitsa kuti agawe uthenga wa Khristu ndi anthu ena. Zotsatira zake, "Ambuye anawonjezera tsiku ndi tsiku amene amapulumutsidwa" (Mach. 2:47).[9]

Zotsindika khumi izi za atumwi mu mpingo mu Yerusalemu zitha kugwira ntchito ngati zotengerapo kwa monga Mbusa wa Chipentekoste lerolino. Zikuthandizirani kuyikiza utumiki wanu ndi mautumiki a Yesu ndi atumwi. Zikuthandizirani kuti mpingo omwe mukutumikira ukhale mphamvu ya uzimu mu dera lanu komanso ndi dziko lonse.

Zolimbikitsa Mbusa ndi Kukhulupirika

Ngati Mbusa wa Chipentekoste, *zomwe* umachita ndizofunikira; *chifukwa* chochitira zinthu ndizofunikiranso kwambiri. Petro adalemba zokhudza zilimbikitso za ntchito ya ubusa (1 Pet. 5:2-3). Abusa asachite ntchito yao kuchokera mkukakamizidwa, kapena kufuna kupeza ndalama, kapena chikhumbokhumbo chofuna kulamulira anthu. Koma, iwo ayenera kusamalira anthu mu zenizeni ndi kuwatumikira. Abusa omwe amatumukira kuchokera ku zokhumba zabwino adzalandira mphoto. Petro akulimbikitsa abusa okhulupirika:

[8] Pa zambiri zokhudza kutsogolera mpingo mukulambira, onani Mutu 18: "Kutsogolera Mpingo M'kulambira."

[9] Pa zambiri zokhudza kubweretsa pamodzi mpingo kuchitira umboni, onani Mutu 37: "Kulalikira Otayika."

"Ndipakuonekera Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero, wosafota" (v. 4).

Ngati Mbusa wa Chipentekoste, musamayiwale kuti tsiku lina mudzaima pamaso pa Khristu kuti mudzapereke mndandanda wa mmene munakwaniritsira mayitanidwe anu. Paulo akutiuza, "Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa kumpando wakuweruza wa Khristu kuti yense alandire zochita m'thupi, monga momwe anachita, kapena chabwino kapena choipa" (2 Ako. 5:10). Mbusa wokhulupirika adzalandira mphotho (Mat. 25:23); Mbusa osakhulupirika adzayesedwa mlandu. (v. 26).

M'malemba onse, woyang'anira omwe alephera kusamalira bwino anthu a Mulungu amaweruzidwa. Mwachitsanzo, Mulungu adayankhula kudzera mwa Yeremiya kuti, "Tsoka abusa amene athetsa nabalalitsa nkhosa za busa langa!…chifukwa mwabalalitsa zoweta zanga ndi kuzipitikitsa ndipo simunazizonda, taonani ndidzakusenzani inu kuipa kwa ntchito zanu, ati Yehova" (Yer. 23:1-2; fanizilani Eze. 34:1-10).

KUPATSIDWA KUTHEKERA KWA UTUMIKI

Utumiki wa ubusa ndi chochitika chakuya cha uzimu. Kuti alalikire anthu otayika ndi kukonzekeretsa oyera mtima, Mbusa wa Chipentekoste, aphunzire kudalira zida zoperekedwa zochokera kwa Mulungu. Koposa, utumiki wa ubusa umaphatikizapo nkhondo ya Uzimu yomwe iyenera kumenyedwa ndi zida za uzimu (Aef. 6:12; 2 Ako. 10:4-5).[10]

Imodzi mwa zida za uzimu zimenezi ndi mphamvu yomwe mudalandira pamene munabatizidwa ndi Mzimu Woyera. Asanabwerere kumwamba, Yesu adalamulira ophunzira ake kuti akhalebe mu Yeruasalemu kuti apatsidwe mphamvu ndi Mzimu Woyera (Mach. 1:4-8). Samayenera kuyamba mautumiki ao kufikira "atavekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba" (Luka 24:49). Iwo analandira mphamvu imeneyo pa Tsiku la Pentekoste pamene "onse anadzazidwa ndi mzimu woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu Woyera anawalankhulitsa" (Mach. 2:4). Monga atumwi, simungathe kukwaniritsa bwino udindo wanu ngati Mbusa popanda kuthekeretsedwa ndi Mulungu. Ndi monga iwo, muyenera kuonetsetsa kuti aliyense amene wabwera kwa Khristu

[10] Pa zambiri zokhudza nkhondo ya uzimu, onani Mutu 22: "Kumenya Nkhondo za Uzimu."

wabatizidwa ndi mzimu Woyera posakhalitsa ndikupatsidwa mphamvu ngati mboni ya Khristu.[11]

[11] Pa zambiri zokhudza kutsogolera ena ku ubatizo wa Mzimu Woyera, onani Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira Ku Ubatizo wa Mzimu."

~ Mutu 24 ~

Kusamalira Nkhosa

Ena mwa Afarisi kamodzi adamunenapo Yesu chifukwa choyanjana ndi anthu otayika. “Uyu alandira anthu ochimwa nadya nao,” anadandaula. Pakumva zonena zao Yesu adafunsa iwo, “Munthu ndani wa inu ali nazo nkhosa makumi khumi, ndipo pakutayika imodzi ya izo,sasiya nanga m’chipululu zinazo makumi asanu ndi anai mphambu zisanu ndi zinai, nalondola yotayikayo kufikira ayipeza? Ndipo pamene adaipeza, aisenza pa mapewa ache wokondwera. Ndipo pakufika kunyumba kwache amema abwenzi ake ndi anasi ake, nanena nao, kondwerani ndi ine, chifukwa ndinapeza nkhosa yanga yotaika!” (fanizilani Luka 15:4-6).

Davide asanakhale mfumu komanso wolemba masalimo, anali Mbusa, wosamalira nkhosa za atate wache. Mkatikati mwa izi, anaphunzira kukonda iliyonse ya iwo. Iye adafika pozindikira kuti Mulungu adamkonda ndi kumusamalira monga m’mene iye asamalira nkhosa zake. Adalemba, “Yehova ndiye mbusa wanga: sindidzasowa. Andigonetsa ku busa lamsipu; anditsogolera ku madzi odikha. Atsitsimutsa moyo wanga” (Masalimo 23:1-2).

Yesu anadzitcha yekha ndi dzina loti Mbusa. “Ine ndine Mbusa Wabwino; ndipo ndizindikira zanga, ndi zanga zindizindikira Ine...ndipo nditaya moyo wanga chifukwa cha nkhosa” (Yohane 10:14-15). Wolemba buku la Ahebri akumutcha Yesu “Mbusa wamkuru wa nkhosa” (Ahebri 13:20). Nkhosa zake ndi iwo amene asankha kumutsata Iye. Yesu akupitiliza kufotokoza kuti Iye ndi mwini nkhosa. Motsutsana ndi wochita kulembedwa ntchito, amene amathawa pamene

nkhandwe yadza kulikhwira nkhosa, mbusa weniweni amaimabe ndikutchinjiriza nkhosa. Iye ndiwokonzeka kupereka moyo wake chifukwa cha izo.

Ngati mbusa wa Chipentekoste, muyenera kumuona Yesu ngati chitsanzo chanu. Muyenera kubusa anthu a Mulungu monga Yesu mwini akadazibusa iwo akadakhala kuti alipo pano kuthupi. Mutuwu ukamba za udindo wa Mbusa wa Chipentekoste kukusamalira nkhosa za Mulungu.

MTIMA WA MBUSA

Ngati Mbusa wa nkhosa za Mulungu, abusa a Chipentekoste ayenera kukhala achifundo, okhulupirika, odalilika, mongatsatanetsataneyu afotokozera:

Wachifundo

Kuyankhula za Mulungu, Yesaya analemba, "Iye adzadyetsa nkhosa zake ngati mbusa, nadzasonkhanitsa ana a nkhosa m'manja mwake, nadzawatengera pa chifuwa chake" (Yes. 40:11). Ngati Mbuye wao, abusa enieni a Chipentekoste ndi achifundo. Amakondadi anthu. Izi zikuphatikizapo iwo ali mkati ndi iwo ali kunja kwa mpingo. Baibulo limati za Iye, "Koma Iye poona makamuwo, anagwida m'mtima ndi chisoni chifukwa cha iwo, popeza anali okambululudwa ndi omwazikana, akunga nkhosa zopanda mbusa (Mat. 9:36). Momwemo, muyenera mu choonadi kukonda anthu amene Mulungu wakuyitanirani kuti muwatumikire.

Wokhulupirika

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kukhala wokhulupirika. Muyeneranso kufunitsitsa kutaya zonse ndi kumutsata Mbuye wanu kwathunthu (Mat. 19:21; Marko 8:34-35). Khristu wayika anthu Ake mmanja mwanu ngati chidaliro chapadera. Muyenera, choncho kusiya zabwino zoyenera inu. Ndipomokhulipirika muyenera kutumikira iwo amene Khristu waikiza pansi pachisamaliro chanu. Paulo analemba zokhudza otumikira uthenga wabwino, "Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale okhulupirika (1 Ako. 4:2).

Wodalilika

Chotsiriza, kuti nkhosa za Mulungu zisamalidwe mokhulupirika, muyenera kukhala wodalilika. Musakhale ngati wochita kulembedwa ntchito, amene mavuto akadza, amasiya nkhosa ndikuthawa (Yohane 10:12-13). Koma, mukhale

okhazikika ndi wodalilika. Kwa Mulungu komanso anthu amene mumawatumikira, athe kudalira inu, kudziwa kuti, patabwera kalikonse, mutha kuwerengedwa ndi kukwaniritsa udindo wako.

NTCHITO YA MBUSA

Ngati Mbusa wake wa Mulungu, Mbusa aliyense wa Chipentekoste amasenza maudindo awiri odziwikiratu: kusamalira nkhosa ndi kukonza mpingo ngati dera losamalira. Tiyeni tiwone maudindo awiri amenewa:

Kusamalira Nkhosa

Choyamba, muyenera kusamalira za nkhosa. Kuti muchite izi, muyenera kukwaniritsa maudindo asanu ndi chimodzi:

1. Kudyetsa nkhosa. Uthenga wa Yesu kwa Petro unali, "Ngati undikonda Ine…dyetsa nkhosa zanga" (Yohane 21:17). Mulungu adalonjeza kwa Israele, "Ndipo ndidzakupatsani inu abusa monga mwa mtima wanga, adzakudyetsani inu nzeru ndi luntha" (Yer. 3:15). Choncho muyenera kudyetsa anthu a Mulungu. Muyenerakuwaphunzitsa Mau a Mulungu mokhulupirika. M'chitidwe uwu upangitsa anthu kuti akule ndi kukhala amphamvu m'chikhulupiro. Zipangitsanso mpingo kumangidwa ndi kukhala okhwima mwa Khristu (Aefeso 4:11-16). Izi, mosakaika konse, ndi zomwe Paulo anamulimbikitsa Timoteo "Lalikira mau; chita nao pa nthawi yake, popanda nthawi yake. Tsutsa, dzudzula, chenjeza, ndikuleza mtima konse ndi chiphunzitso" (2 Tim. 4:2).

Osati mungoyenera kukhulupirika pa kulalikira ndi kuphunzitsa Mau a Mulungu, muyeneranso kukhazikitsa dongosolo lomveka lakaphunzitsidwe mu mpingo. Muonetsetse kuti Baibulo likuphunzitsidwa mwadongosolo kwa anthu a zaka zonse—ana, achinyamata, ndi akulu.[1]

2. Kuteteza nkhosa. Paulo adauza akuluakulu a ku Aefeso, "Tadzichenjerani nokha ndi gulu la nkhosa lonse, pamenepo Mzimu Woyera anakuikani woyang'anira" (Mach. 20:28). Kenako adawachenjeza, "Ndidziwa ine kuti, nditachoka ine, adzalowa mimbulu yosautsa, yosalekerera gululo; ndipo mwa inu

[1] Pa zambiri zokhudza udindo wa mbusa wa Chipentekosite mu kuphunzitsa Mau a Mulungu, onani Mutu 17: "Kuphunzitsa Kwabwino"

nokha adzauka anthu, olankhula zokhotakhota, kupatutsa ophunzira awatsate. Chifukwa chake dikirani!" (vv. 29-31).

Muyenera kukhala ochilimika motsutsana ndi aneneri abodza ndi aphunzitsi abodza amene amafuna kulikwira pa mpingo. Muyenera kuwazindikira awa "nkhandwe mchovala cha nkhosa" ndi kuwadzudzula mwa mphamvu. Ngati kuli kotheka, pamodzi ndi utsogoleri wa mpingo, muyenera kuwachotsa pakati pa anthu. Muyenera kuchita chimodzimodzi ndi onse obweretsa mavuto nthawinthawi akupangitsa mgawano mu mpingo (Aro. 16:17).

Kuphatikiza apo, muyenera kuteteza anthu a Mulungu kuchokera ku ziphunzitso za bodza ndi aphunzitsi onyenga pakuwaonetsera choonadi. Pamenepo iwo, "Sadzakhalanso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengekatengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitso, ndi tsenga la anthu ndi kuchenjerera kutsata chinyengo chakusocheretsa. Koma ndi kuchita zoona mwachikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu" (Aefeso. 4:14-15).[2]

3. Kufikira iwo akupwetekedwa. Yesu adafikira ndi mtima wa chisoni ku anthu opwetekedwa (Mat. 9:36; 15:32-38). Ngati Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuchita chimodzimodzi. Muyenera kufikira mwa chikondi kwa ofooka ndi ovutika mu mpingo ndi dera lanu. Izi zitha kuphatikizapo amayi amasiye ndi ana amasiye (Yakobo 1:27). Zitha kuphatikizaponso odwala, osauka, iwo ali mu ndende, ndi ena osowa (Mat. 25:38). Yesu akutilimbikitsa, "Indetu ndinena kwa inu, chifukwa munachitira ichi mmodzi wa abale anga, ngakhale ang'onoang'ono awa, munachitira ichi Ine" (v. 40).

Muyenera kuyendera nyumba za iwo amene ali odwala,okhumudwitsidwa, obwerera m'mbuyo, kapena ozunzidwa ndi ziwanda. Kumeneko, mukatumikira molingana ndi chosowekacho. Muyeneranso kuyendera ma membala omwe ali m'chipatala kapena kumangidwa ku ndende. Muyenera kutenga nthawi kuwapempherera ndi kuwalimbikitsa. Muthanso kuyika nthawi yachindunji ku ofesi yomwe mudzilandira anthu amene ali mmavuto osiyanasiyana kapena zina

[2] Pa zambiri zokhudza kuteteza mpingo, onani Mutu 27: "Kuteteza Nkhosa."

zofuna uphungu. Kumeneko, mukamva mwatcheru mavuto ao, kupemphera nao, ndi kuwathandiza kupeza mayankho m'Mau a Mulungu.[3]

4. Kulimbitsa ofooka. Mu mpingo muli iwo amene ali ofooka mu uzimu. Chifukwa cha ichi, mayendedwe ao ndi Ambuyendiwosakhazikika. Ena, chifukwa cha kusakhwima mu uzimu wao, kapena zifukwa zina, ali muchiopsezo chakupatuka panjira yaAmbuye. Nthawi ndi nthawi mudzikhala oyang'anitsitsa kupeza anthu amene ali munyengo zowawazi. Muyenera kupeza njira zowalimbikitsa ndi kuwathandiza m'mayendedwe ao ndi Ambuye. Njira ina yowalimbikitsa ndikuwapatsa mmodzi wa akhristu okhwima kuti akhale anzao ndi kuwalimbikitsa. Njira inandikuonetsetsa kuti iwo adzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mzimu adzakhala mthandizi, mtonthozi, komanso wotsogolera.[4]

5. Kufuna Otayikawo. Yesu adachita umboni kuti Iye anadza "Kufunafuna ndi kupulumutsa chotaikacho" (Luka 19:10). Iye adalamulira ophunzira ake kuti achite zomwezo (Marko 16:15-16; Luka 14:23). Ngati mbusa wa Chipentekoste, muyenera kutsatira chitsanzo cha Ambuye wathu. Tumikirani otayika, ndikuwatsogolera kuti achite chimodzimodzi. Kupitirira apo, konzani, mpingo wanu ku kulalikira kwa mphamvu ya Mzimu, kudzala mipingo, ndi kuchita utumwi.

Kuti muchite izi mukufunikira kulalikira ndi kuphunzitsa nthawi zambiri zakufunikira kwa anthu kuti amudziwe Khristu ngati Mpulumutsi. Komanso mudziwakumbutsa anthu a Mulungu pafupipafupi za udindo wao wakufikira otayika ndi uthenga wabwino. Mukhazikitse madongosolo ndi zoyambitsa zina kuti mulimbikitse ndi kukonzekeretsa anthu kuchitira umboni. Wina wanena molondola kuti, "Njira yabwino yakuti Mbusa alimbikitse anthu ake kukuchitira umboni ndikukhala iye wochitira umboni." Pamene anthu akuona Mbusa wao akupambana mu kufikira otayika, ndikuwabweretsa ku mpingo, iwo atakasika ndikuchita zomwezo.[5]

6. Kupereka mwambo kwa opulupudza. Mwambo ndi mbali yofunikira kwambiri pakusamalira nkhosa. Ndi njira yofotokozedwa ya m'baibulo kuyitana

---

[3] Pa zambiri zokhudza utumiki ma uphungu wa Mbusa wa Chipentekosite, onani mutu 26: "Kupereka Uphungu kwa Anthu a Mulungu."

[4] Pa zambiri zokhudza kutsogolera ma membala mu chidzalo cha Mzimu , onani Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira Mu Ubatizo Wa Mzimu."

[5] Pa zambiri zokhudza kufikira otaika onani mutu 37: "Kulalikira Otayika" ndi Mutu 39: "Kudzala Mipingo Yatsopano."

iwo akusochera kubwereranso mu gulu la nkhosa. Pamene mamembala opulukira achita tchimo lowonekeratu, achenjezedwe. Ngati alape, mbale kapena mlongo wabwezeretsedwa kwa Khristu. Ngati akane kulapa, adzapatsidwa mwambo (Mat. 18:15-17). M'chitidwe uwu ukwaniritsa zinthu ziwiri; utumikira pakudzutsanso obwerera m'mbuyo, komanso utumikira ngati chenjezo kwa ena mu mpingo.

Kumbukirani, cholinga cha kupereka mwambo nthawi zonse ndi kuombola. Muyenera kuchita izi mu mzimu wakuzichepetsa ndi chikondi. Paulo akulemba, "Abale, ngatinso munthu agwidwa nako kulakwa kwakuti, inu auzimu, mubweze wotereyo mu mzimu wa chifatso. Ndi kuzipenyerera wekha, ungayesedwe nawenso" (Agal. 6:1).

Kulenga Dera Losamalirana

Ngati mbusa wa Chipentekoste, osati udzingosamalira anthu kokha, monga zanenedwa mwambamu, muyenera kulimbikitsa mpingo kuchita chimodzimodzi. Muyenera kufunitsitsa kuwumba mpingo wanu kukhala dera losamalirana. Kukhala dera losamalirana zikutanthauza kuti mitima ya mamembala yadzala ndi kumva chisoni chifukwa cha anthu opwetekedwa. Chifukwa kuti ndi odzala ndi chikondi cha Mulungu, iwo amafikira anthu osoweka mosavuta. Akaona m'bale kapena mlongo opwetekedwa,mwachangu amavomereza ndi kukhudzidwa. Izi ndi zomwe Yesu anachita pamene anakumana ndi munthu wakhate. Munthuyo anati kwa Yesu, "Ngati mufuna mukhoza kundikonza." Baibulo likutiuza, "Ndipo Yesu anagwida ndi chifundo, natansa dzanja namkhudza iye, nanena naye "Ndifuna; Khala wokonzedwa!" (Marko 1:40-42).

Njira imodzi youmbira anthu a Mulungu kukhala dera losamalira ndi kuonetsetsa kuti adzazidwa ndi Mzimu Woyera ndikuti Mzimuyo akugwira ntchito mwamphamvu miyoyo yao. Chikondi ndi chipatso cha Mzimu (Agal. 5:22). Baibulo limati, "Chikondi cha Mulungu chatsanulidwa m'mitima mwanthu mwa Mzimu Woyera amene wapatsidwa kwa ife" (Aro. 5:5). Komanso, pamene anthu achita chifundo choonetsa ndi moyo wa mbusa, adzakhalanso a chifundo iwo eni.

Mmene nyengo ifunire, ndi momwe Mzimu atsogolera, mutha kufuna kutsogolera mpingo pakukhazikitsa dongosolo la zachifundo. Izi zitha kuphatikizapo kudyetsa, kumanga, ndi madongosolo ena.[6]

KUKHULUPIRIKA KWA MBUSA

Monga zanenedwa mwambamu, Mbusa wa Chipentekoste adzione yekha ngati oyang'anira kapena osamalira mpingo wa Khristu. Abusawa asamayiwale kuti mpingo si wao; ndi wake wa Khristu. Ngati oyang'anira mpingo Wake, iwo amafunsidwa ndi Iye. Mokhulupirika agwire ntchito yao, popeza tsiku lina pamene Khristu adzabwera, adzafunsidwa mmene adachitira katundu Wake (Luka 12:42-43; 1 Ako. 4:2).

Abusa otumikira modzikonda ndi kusalabadira za nkhosaadzaweruzidwa moipa. Mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano zonse, Baibulo limatsutsa abusa otere mwamphamvu. Mwachitsanzo, Ezekiele adanenera motsutsana ndi abusa otere amene amadzinenepetsa okha mmalo mwa nkhosa: "Zofooka simunazilimbitse; yodwala simunaichiritse, yothyoka simunailukire chika, yopirikitsidwa simunaibweze, yotaika simunaifune" (Eze. 34:4). Kenako kuyankhula kudzera mwa Mneneriyo, Mulungu adalengeza, "Ine ndiipidwa nao abusa, ndidzafunsa nkhosa zanga pa dzanja lao" (v. 10). Panthawi ina, Mulungu adaweruza abusa a Israele, "Mwabalalitsa zoweta zanga, ndi kuzipirikitsa, ndipo simuzizonde; taonani, ndidzakusenzani inu kuipa kwa ntchito zanu" (Yer. 23:2).

Mu Chipangano Chatsopano, Yakobo akuchenjeza, "Musakhale aphunzitsi ambiri, abale anga, podziwa kuti tidzalangika koposa" (Yakobo 3:1). Petro akulemba zokhudza aneneri ndi aphunzitsi onama, "Amene adzalowa nayo m'tseri mipatuko yotayikitsa, nadzakana Ambuye amene adawagula—nadzadzitengera iwo okha chitayiko chakudza msanga" (2 Pet. 2:1).

Pamene Mulungu adzaweruza abusa osakhulupirika, adzapereka, mphotho moyenera iwo amene amasamalira nkhosa mokhulupirika. Yesu anati, "Ndani kodi ali kapolo wokhulupirika ndi wanzeru, amene mbuye wake anamkhazika woyang'anira banja lake, kuwapatsa chakudya mu nthawi yake? Wodala kapolo amene mbuye wache, pakufika, adzampeza iye akuchita chotero. Indetu, ndinena kwa inu, kuti adzamkhazika iye woyang'anira zinthu zake zonse" (Mat. 24:45).

[6] Izi zakambidwa mochuluka mu Mutu 38: "Kutumikira Dera Lanu."

Kulembera kwa akuluakulu a mipingo, Petro akulimbikitsa, “Wetani gulu la Mulungu lili mwa inu, ndi kuliyang’anira, osati mokakamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyasa, koma mwachangu; osati monga ochita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo” (1 Pet. 5:2-3). Kenako anawalimbikitsa iwo, kunena kuti, “Ndipo pakuoneka Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero wosafota” (v. 4).

Kutumikira Khristu ngati mbusa pa nkhosa zake ndi kuphatikizapo ulemu ndi udindo wopatulika. Abusa omwe akwanilitse ntchito zao mokhulupirika atha kuyang’ana kutsogolo ndi chiyembekezo ndi chimwemwe chachikulu. Tsiku lina adzamva mau a Mbuye wao, “Chabwino, kapolo iwe wabwino ndi okhulupirika; unali wokhululpirika pa zinthu zazing’ono ndidzakhazika iwe pa zinthu zambiri; lowa M’chikondwerero cha mbuye wako!” (Mat. 25:21).

~ Mutu 25 ~

Kulimbikitsa Thupi La Khristu

Mlaliki wina wodziwa anachititsa msonkhano wolalikira waukulu m'chigawo chapakati mu Afirika. Mazanamazana a anthu anabwera ku msonkhanowo, ndipo mazana a anthu anavomera kumuitano wa kulandira Khristu ngati Mpulumutsi. Kunali chimwemwe chachikulu komwe msonkhanowu umachitikira.

Patadutsa zaka zitatu, kafukufuku wa zotsatira adachitika.Zinazindikirika kuti mwa anthu zikwizikwi ovomereza chikhulupiriro, ochepa okha ndi amene anali kupezeka m'mipingo. Pakumva izi, mmodzi mwa atsogoleri a mpingo, "Mtima wanga udavutika pakumva za zotsatirazo. Mkati mwa mzimu wangandinamva kuti mpingo mu Afirika ukuyenera kuonanso njira zake zakupangira ophunzira a Yesu. Mpingo wa Chipentekoste mu Afirika ufike pozindikira kuti kufalitsa uthenga wabwino zikuphatikizapo ntchito yakuphunzitsa ophunzira."

Mpingo wa Chipentekoste mu Afirika ndi odziwika ndikupambana pa kulalikira kwake. Uyenera tsopano kudziwika ndi madongosolo ake a kuphunzitsa. Kulalikira ndi kuphunzitsa zimayenda limodzi. Abusa a Chipentekoste asangokhudzidwa ndikuti angakuze bwanji mpingo, koma ayenera kudziperekanso kukulimbitsa mpingo. Mutu uwu tikambirana njira zitatu zomwe, inu ngati mbusa wa Chipentekoste, mungalimbikitsire thupi la Khristu.

UDINDO WA MBUSA WA CHIPENTEKOSTE

Udindo wa ukulu wa Mbusa aliyense ndi kuumba ndi kulimbikitsa mpingo omwe akuwutsogolera. Choncho Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kulunjika kusiya mpingo uli wamphamvu kuposa mmene anaupezera. Njira yoyambirira yomwe Mbusa atha kufikira cholinga ichi ndikudzera m'kuphunzitsa ophunzira. Ntchito iyi ili pa mtima pa lamulo lalikulu kapena kutuma kwakulu, pomwe Yesu adalamulira ophunzira ake "Mukani,phunzitsani anthu a mitundu yonse" (Mat. 28:19). Amawauza iwo kuti achite ndi ena zomwe Iye wachita ndi iwo. Monga Iye, amayenera kulunjika nthawi yao ndi mphamvu zao mu kuumba gulu lomwe likhudze maiko. Paulo anatsindika za ndondomekoyi pameneanamulangiza Timoteo, "Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika amene adzadziwa kuphunzitsa enanso" (2 Tim. 2:2).

Kulimbikitsa Mpingo

Paulo anatenga lamulo la Yesu kupanga ophunzira mwa chidwi. Mbali yofunika kwambiri mu utumiki wake inaperekedwa mukulimbikitsa mipingo yomwe anadzala. Ichi nchifukwa chake iye amasakha abusa m'mipingo iliyonse (Mach. 14:23), kuyiyendera mipingo yomwe iye wadzala (15:41), ndikulemba makalata otsatila iwo kuwalangiza iwo njira za Ambuye. Paulo kupitirira apoakuchitira umboni kuti Ambuye anampatsa iye ulamuliro wa utumwi kuti amange mipingo (2 Ako. 10:8; 13:10). Ngati Mbusa wa Chipentekoste, muwone utumiki wanu mu njira yomweyo. Mudzione nokha ngati wopanga ophunzira wamkulu mu mpingo omwe Khristu wakupatsani kuti mutsogolere.

Mu kalata yake kwa akhristu a ku Aefeso, Paulo akuti Khristu anapereka abusa (pamodzi ndi ma utumiki ena anai) kukumangirira thupi la Khristu (Aef. 4:11-16). Mu ndimeyi, mtumwi akulemba kuti otumikirawa ntchito yao yoyamba ndi "Kukonzekeretsa oyera mtima ku ntchito ya utumiki." (v. 12). Ayenera kuchita izi "kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupirio… ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khritsu " (vv. 12-13). Kenako, Paulo akufotokoza, mpingo "Ukula m'zinthu zonse, kufikira Iye amene ali Mutu ndiye Khristu" (v. 15).

Kupanga ophunzira ndikofunikira ku mpingo uliwonse omwe ukhale wathanzi. Ngati utsogoleri wa mpingo ulephere kupanga ophunzira, kulimbikira kwao pa kulalikira ndi kudzala mipingo zikhala pachabe.

Kumvetsetsa Mawu

Kuti timvetsetse bwino njira yopangira ophunzira, ndi zofunikira kumvetsetsa mawu amene akugwiritsidwa ntchito. Tiyeni tione atatu mwa mawuwa:

1. Ophunzira. Ophunzira ndi odzipereka kumaphunziro. Iye ndi amene amakhala mwatcheru pamapazi a mphunzitsi wake kumwa ku mau ao. Monga wophunzira, iye amaphunzira zochita pakutsanza mmisiri waluso. Wophunzira wa Khristu ndi munthu amene wapereka moyo wake kwa Yesu Khristu ndipo tsiku ndi tsiku akutsanza Iye, kuphunzira kwa Iye, ndikutsatira cholinga cha Iye.

2. Kuphunzitsa. Kuphunzitsidwa ndi ndondomeko yamoyo yaitali yakukhala ngati Yesu. Imayamba nthawi imene munthu wapereka moyo wake kwa Khristu ndipo akupitiliza kufikira imfa. Ganizo la kuphunzitsidwa ndi mutu waukulu mu Chipangano chatsopano. Pamene liwu lakuti *Khristu* likuonekera katatu kokha mu buku la Machitidwe, ndikuti liwu lakuti *wokhulupirira*likuonetsedwa kochuluka ka 35 mu Uthenga Wabwino komanso Machitidwe, liwu lakuti wophunzira likupezeka kochuluka 289 mu Uthenga Wabwino komanso ka 13 mu Machitidwe.

Kuphunzira zimafunika kudzipereka kwa Khristu ndi kucholinga chake. Yesu adachenjeza khamu lomutsata Iye, “Ndipo aliyense sasenza mtanda wake wa mwini yekha, ndikudza pambuyo panga, sakhodza kukhala wophunzira wanga” (Luka 14:27). Adawauza iwo kuti ayenera kudziwa dipo lake asadayambe kumutsata iye. Adawachenjeza, “Chifukwa chake tsono, yense wa inu amene sakaniza zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga” (v. 33).

3. Wopanga Wophunzira. Wopanga wophunzira ndi amene ali wodzipereka kukumvera lamulo la Khristu, “Kupanga ophunzira mitundu yonse” (Mat. 28:19). Iye ali otsatira wokhwima wa Khristu amene adzipereka kutsatira kwathunthu Mbuye wake ndikutsogolera zomwezo ena. Abusa a chipentekoste mwamphamvu amvetsetse kuti ntchito yawo sikungopanga ophunzira okha. Ntchito yawo ndikupanga ophunzira kufikira akhale ophunzira odzipereka kwathunthu kwa Khristu.

NJIRA ZA KULIMBIKITSIRA MPINGO

Khristu sadafune kuti ntchito ya ufumu wa Mulungu ichitidwe ndi abusa odziwa okha. Koma Iye anapereka mphatso za utumiki zisanu ku mpingo kuti ziphunzitse akhristu tsiku lililonse moyo ndi ntchito ya mu ufumu. Cholinga cha atumwi, aneneri, alaliki, abusa, ndi aphunzitsi ndi kukuza akhristu kukhala opindula miyoyo, komanso kuti awaphunizitse mmene angasamalilire wina ndi mzake ndi kukuza wina ndi mzake kukhala atumiki amphamvu a Khristu. (Aef 4:11-16).

Choncho, monga Mbusa wa Chipentekosite, muyenera kuphunzitsa kuti yense wotsatila Khristu waitanidwa ndi kupatsidwa kuthekera kuti atenge mbali mu kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu padziko lapansi. Pamene ochepa chabe ayitanidwa kuti akhale atumwi, onse akuyitanidwa kutenga mbali mu utumwi. Pamene ochepa ayitanidwa kukhala aneneri, onse ndi oyitanidwa kuti akaime chifukwa cha chabwino ndi cholondola. Pamene ochepa ayitanidwa kukhala alaliki, onse ndi oyitanidwa kugawana ndi ena chikhulupiriro chao. Pamene ochepa ayitanidwa kukhala aphunzitsi, onse ndi oyitanidwa kuphunzitsa ena kuti atumikire Khristu. Pamene ochepa ayitanidwa kukhala abusa, onse ndi oyitanidwa ku kusamalira chifukwa cha ena. Ngati Mbusa, ntchito yanu ndi kuphunzitsa zinthu izi kwa anthu a Mulungu ndikukuza ndondomeko ya maphunziro ya mphamvu mu mpingo.

Tiyeni tione ndondomeko zisanu n'chimodzi yomwemungagwiritse ntchito kulimbitsa mpingo wanu:

Kuonetsera Moyo wa Ophunzira

Choyamba, mutha kulimbikitsa mpingo pa kukhala chomwe chimatanthauza ophunzira wa Khristu. Ndi moyo wanu omwe, mutha kuonetsera momwe wophunzira wa Khristu amaonekera. Pamene membala wa mpingo awona moyo wa umulungu wa Mbusa wao, adzalimbikitsika kuti akhale momwemo. Iwonso adzafuna kukhala ophunzira a Khristu. Zotsatira zake, mpingo udzakula mwa mphamvu ndi kupambana, ndi ufumu wa Mulungu udzapita patsogolo.

Ndondomeko ya kuphunzitsa ndiyofunikira makamaka mukukhazikitsa mipingo yatsopano mu madera omwe sadafikiridwe. Mu nyengo ngati izi, akhristu atsopano ali ndi chidziwitso chochepa ku zomwe zimatathauza kukhala ndi moyo chifukwa cha Khristu. Chitsanzo chomwe iwo ali nacho ku moyo wachikhristu ndi

moyo wa mbusa ndi banja lake. Ngati Paulo, muyenera kukhala okonzeka kunena ku anthu, "Khalani onditsanza ine, monga inenso nditsanza Khristu" (1 Ako. 11:1).

Kulalikira ndi Kuphunzitsa

Chachiwiri, mutha kulimbikitsa thupi kudzera munjira zolalikira ndi ndondomeko ya kaphunzitsidwe ka Mau a Mulungu. Kulalikira Mau a Mulungu mwandondomeko ndikukonzekera ndi kulalikira mauthenga a Baibulo ndikulunjika komveka bwino m'malingaliro. Kuti tichite izi, choyamba muyenera kudziwa, kudzera mpemphero ndi kulingalira pa Mau a Mulungu, chitsogozo chomwe Mzimu woyera akutsogolera mpingo. Pamene mukudikira mpemphero, Mzimu Woyera adzayankhula mu mtima mwanu kuti, "Njira ndi iyi; yendani inu mmenemo" (Yes. 30:21).[1]

Pamene mwazindikira chitsogozo cha Mulungu pa mpingo, yambani kukonzekera ndi kulalikira mauthenga ndicholinga chobweretsa mpingo kuchitsogozocho. Nthawi yomweyo, muwonetsetse kuti "uphungu wonse wa Khristu" kutanthauza Mau a Mulungu onse akuphunzitsidwa mu mpingo (Mach. 20:27). Chikhalidwe chonga ichi chidzapangitsa kuti anthu a Mulungu amvetsetse Mau a Mulungu ndi chifuniro chake ku moyo wao. [2]

Kuphatikiza apo, ziphunzitso ndi zolalikira zanu zikhale ndi maunthenga okhudza utumwi wa Mulungu pafupipafupi, pamodzi ndi udindo wa mpingo kutenga mbali ku ntchito imeneyo. Ntchito ya Mulungu, nthawi zina imatchedwa *missio Dei,* lomwe ndi dongosolo la Mulungu kuwombola ndi kudziyitanira yekha anthu kuchokera ku mtundu, ziyankhulo, ndi mafuko onse pa dziko lapansi. (Chiv. 5:9; 7:9). Yesu anatsimikizira za udindo wa mpingo mukukwaniritsa ntchito Yake mu Lamulo Lalikulu. (Mat. 28:18-20; Marko 16:15-18; Luka 24:46-49; Yohane 20:21-22; Mach. 1:8).

---

[1] Pa zambiri zokhuda mutuwu, onani Mutu 15: "Chizolowezi Chodzipereka Champhamvu."

[2] Pa zambiri zokhudza mutuwu, onani Mutu 16: Kulalikira Modzozedwa ndi Mzimu" ndi Mutu 17: "Kuphunzitsa Kwabwino." Mabuku a "Kukhala Choonadi" ndi "Muzu wa Chikhulupiriro," Maphunziro a ophunzitsa atha kupezeka mwaulele pa tsamba la www.africaatts.org/resources.

Kupereka Mphamvu kwa Anthu

Chachitatu, mutha kulimbikitsa thupi pakuonetsetsa kuti mamembala a mu mpingo apatsidwa mphamvu kukutumikira. Kupereka mphamvu kumeneku kumaphatikizapo za uzimu komanso malingaliro:

Kupatsidwa mphamvu za uzimu. Gwirani ntchito kufikira mutaona membala aliyense mu mpingo atapatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Ili linali lamulo lotsiriza la Yesu ku mpingo. Atatsala pang'ono kuti akwere kumwamba, adalamulira ophunzira ake, "Musachoke ku Yerusalemu, koma alindire lonjezano la Atate,limene anati, munalimva kwa ine. Pakuti Yohane anabatiza ndi madzi; koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera asanapite masiku ambiri" (Mach. 1:4-5). Yesu kenako anapereka lonjezo lodabwitsa kwa ophunzira ake: "Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko." Ophunzira anamvera zomwe Khristu adawalamulira, ndipo Yesu adakwaniritsa lonjezano lake. Baibulo litiuza,

"Ndipo pakufika tsiku la Pentekoste, anali onse pamodzi pa malo amodzi. Ndipo mwadzidzidzi anamveka mau ochokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzadza nyumba yonse anali kukhalamo. Ndipo anaonekera kwa iwo malilime ogawanikana, onga a moto; ndipo unakhala pa iwo onse wayekha. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa." (Mach. 2:1-4)

Kupatsidwa mphamvu yochokera kumwamba ndi chinsinsi cha kulalikira kwa bwino ndi utumwi mu mpingo. Muyenera choncho kulalikira pa mutu uwu ndikupemphera ndi anthu kuti adzazidwe ndi Mzimu Woyera.[3] Kupitirira apo muyenera kuphunzitsa iwo mmene angakhalire ndikuyenda mu mphamvu ya Mzimu. Ndipo alimbikitseni kuti apeza chipatso cha Mzimu komanso kuonetsera

[3] Buku lotchedwa, *Kulalikira Chipentekoste: Ndondomeko zama Ulaliki 100 a Mphamvu ya Mzimu Woyera,* litha kupezeka mwaulere pa tsamba la www.DecadeofPentecost.org. Pa zambiri zokhudza mmene tingawapempherere okhulupirira kulandira Mzimu Woyera, onani, Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

mphatso za Mzimu m'miyoyo ndi mautumiki awo (Agal. 5:22-23; 1 Ako. 12:8-10).[4]

Kupatsidwa Mphamvu mkaganizidwe. Monga mbusa, muyenera kugwira ntchito pakuonetsetsa kuti mamembala anu mu mpingo apatsidwa mphamvu mkaganizidwe kao pa utumiki. Ma membala amapatsidwa mphamvu mkaganizidwe pamene akhulupirira kuti khomo latseguka kuti atenge mbali mu mautumiki a pa mpingo. Apatsidwa kulimbika mtima kuti atha kupambana m'mautumiki omwe asakhidwa. Ngati Mbusa wa Chipentekoste, ndi ntchito yako kuikiza kulimbika mtima kumeneku mwa anthu.

Ngati muchite izi, mamembala a pa mpingo adzalimbikitsa nadzipereka okha ku utumiki. Koma, mukalephera izi, iwo adzakhala onyozera kuti adzipereke. Mupewe, choncho, kuonetsera kuti inu ndinu yekhayo wovomerezeka kugwira ntchito ya utumiki pa mpingo. Koma, tsindikani kuti pali danga la utumiki kwa wina aliyense. Ndipo muyenera kuikiza m'mitima mwa anthu chitsimikizo chakuti atha kutumikira Khristu bwino lomwe.

Kubweretsa Pamodzi Antchito

Pamene anthu apatsidwa kuthekera, aikidwe pamodzi chifukwa cha utumiki. Iyi ndi njira yachinayi yomwe mutha kulimbikitsira mpingo. Ndondomeko yakubweretsa pamodzi ogwira ntchito ili ndi zochitika izi:

Kuzindikira chosoweka. Umayamba njira yakubweretsa pamodziyi pakuzindikira chosowa chomwe mukufuna kuchifikira. Kodi mpingo ukufuna kuyambitsa utumiki watsopano wa ana, kudzala mpingo watsopano, kupititsa patsogolo mapemphero a mpingo, kapena kukwaniritsa ntchito zina? Muyambe ndondomeko ya kubweretsa pamodzi pakufotokozera bwino chomwe mukufuna chitakwaniritsidwa.

Kulenga mwayi wa ntchito. Muyenera kutsimikizika ku ma udindo amene akufunika kukonzedwa kuti zigwiridwe pa utumiki watsopanowo. Muyenera kukonza zofotokozera kagwiridwe kantchito pa udindo watsopanowo. Zofotokozera kagwiridwe kantchito zitha kuphatikizapo zoyenereza komanso zochita za iye amene ali pa udindo.

[4] Pa zakutathauzira mphatso za uzimu, onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

Kupemphera. Nthawi zonse, mudzipemphera kwa Ambuye wa kholola, ku funsa Iye adzutse antchito ofunikirawo (Luka 10:2).

Kugawa masomphenya. Panthawi yoyikika, gawanani masomphenya ndi mpingo. Muyenera kuwauza anthu za utumiki watsopano, kufotokozera m'mene ungadalitsire mpingo.

Kulemba antchito. Muyenera tsopano kufunsa anthu odzipereka. Mukhale a chindunji ku zomwe ntchitoyo ikhazikikepo. Muthanso kuzindikira ena paokha amene mukuganiza kuti atha kugwira bwino ntchito ndikuwafunsa kuti apemphere zokhudza iwo kudzipereka ku ntchitoyo. Funitsitsani kufananiza mphatso ya munthu ndi zomwe ntchito ikufuna.

Kuphunzitsa. Konzani dongosolo la maphunziro kwa iwo amene adzipereka.

Kuyikiza. Pamene mwasankha antchito atsopano, ndipo mwaphunzitsa moyenera, muyenera kuwayika m'maudindo ao. Khalanibe pa ubale ndi antchito atsopanowa, kuyang'anira kachitidwe kao ndikuwalimbikitsa mu ntchito. Mpingo uyenera kupereka zofunikira zomwe iwo akufunikira kuti akwaniritse udindo wao.

Kuphunzitsa za Utumiki

Monga zanenedwa kale, kubweretsa mamembala pa za utumiki, mukhale okonzekera kupereka maphunziro kwa iwo odzipereka.Anthu ndiwofunitsitsa kudzipereka ngati adziwe kuti alandiramaphunziro a ntchito yawo. Maphunziro amachulukitsa chiyembekezo chawo mukupambana. Maphunziro atha kuchitika kudzera m'misonkhano yapadera kapena maphunziro a pantchito pompo. Maphunzirowa akambe *chifukwa* kapena *mmene* wa zokhudza ntchitoyo. Antchito atsopano auzidwe chifukwa chimene utumikiwo ulipo komanso zomwe ukufunikira kuti ukwaniritse. Ayenera kuuzidwanso m'mene angagwirire ntchito mwapamwamba. Mbusa atha kuganizira zakuyambitsa Sukulu ya Utumiki mu mpingo.[5]

Kuthandiza Iwo Amene Akuonetsa Chiyembekezo

Njira yomaliza yomwe mutha kulimbikitsa thupi ndi kuzindikira ndikulingalira za kuthandiza iwo amene akuonetsa chiyembekezo. Monga Mbusa,

[5] Utumiki wafotokozeredwa mu Mutu 17: "Kuphunzitsa Kwabwino."

zindikirani mamembala amene akusonyeza chidwi chachikulu pa ntchito ya Mulungu. Mutha kuzindikira mkono wa Mulungu pa anthu amenewa. Pamene izi zachitika, mutha kufuna kukhazikitsa ubale wakuthandizana ndi iwo, monga Yesu adachitira ndi ophunzira Ake. Pamenepo mudzatha kukhala ndi nthawi ndi iwo, kupemphera nawo komanso kuwayitanira iwo kuti akhale ndi inu m'ntchito zina za utumiki.

Ena azindikira kuti njira ya Yesu pakuphunzitsa imaphatikizapo ndondomeko zitatu: choyamba, Yesu amatumikira kwa ena akuphunzira ake akuona. Nthawi zina amawatengera pa mbalindikuwafotokozera chomwe wachita ndichifukwa chomwe wachitira. Chachiwiri, ophunzira Ake amatumikira Yesu akuona. Kenako pamenepo amayang'na kachitidwe kawo. Chotsiriza, Yesu amatuma ophunzira kukatumikira pa iwo okha ndikukuza ophunzira ena monga Iye adakuza iwo. Analonjeza kutumiza Mzimu Woyera kuwapatsa mphamvu ndikuwathandiza iwo mu utumiki.

Ena mwa iwo mukuwathandiza atha kumamva maitanidwe mu utumiki. Izi zikachitika, mukufunikira kusamalira maitanidwewo. Ndipo mutha kufunanso kuwatsogolera iwo ndondomeko yakuwayenereza ku utumiki.

Baibulo limaphunzitsa kuti mpingo "uchita makulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi, *monga mwakuchititsa kwa chiwalo chonse pa muyeso wake"* (Aefeso 4:16). Njira yabwino ya mbusa wa Chipentekoste kuti alimbikitsire mpingo ndikukuzandondomeko ya mphamvu ya maphunziro yolunjika ku kusintha okhulupirira kukhala ophunzira ndipo ophunzira kukhala otumikira abwino a uthenga wabwino.

~ Mutu 26 ~

Kupereka Uphungu Kwa Anthu a Mulungu

Mmodzi wa mamembala mu mpingo akuganizira zakuthetsa banja patatha zaka zambiri mu ubwenzi wankhanza. Mzibambo wachichepere wamasiye akuvutika chifukwa cha kumwalira kwa mkazi wake. Mzimayi amene ali yekha akulimbana ndi nthenda ya khansa yomwe adapezeka nayo. Makolo osautsidwa akuyesera kuti alamulire mwanawao woukira. Awa ndi ena mwa mazana mazana a nkhani zomwe mamembala a mipingo ya Chipentekoste mu Afirika amakumana nazo. Kuphatikiza ku mndandandawu ndi iwo amene akuvutika ndi kuzunza kwa ziwanda, mliri wa umphawi, kusowa ntchito, zikhalidwe zosokoneza ndi zina zambiri.

Mulungu adamulenga mwamuna ndi mkazi mu m'chifanizo chake. Adalenga Adamu ndi Hava angwiro mthupi, malingaliro, ndi mu mzimu. Iwo anali "Luso la Mulungu" okhala m'chiyanjano ndi Iye komanso wina ndi mzake. Komabe, pamene adachimwa, ubale wao ndi Mulungu, komanso wina ndi mzake, unasokonekera (Gen. 3:6-24; Arom. 5:12). Kusweka mtima ndi kusautsika inakhala mbali imodzi ya moyo wa munthu.

Mbusa kupereka uphungu ndi phata la utumiki wake. Khristu waitanira mpingo wake kuti ukhale malo a chikondi ndi chisamaliro. Akufuna ukhale malo amene anthu Ake akhale pa ubwenzi ndi Iye limodzi ndi Mzimu Woyera

kubweretsa machiritso ndi chidzalo chonse kwa anthu osweka. Akhale malo amene anthu otaika atha kukumana ndikusandulizika, kubwezeretsedwa, ndi chiyembekezo (2 Ako. 5:18-19). Mulungu walamulira mbusa wa Chipentekoste kuti aonetsetse kuti ntchitoyo ikuchitika.

Mutu uwu, tiwona utumiki wa kupereka uphungu wa mbusa wa Chipentekoste mu Afirika. Ufotokozera zikhalidwe zoonera za kupereka uphungu ndikukhazikitsa maziko a Baibulo ku zomwezo. Kupitirira apo ufotokozera ntchito ya Mzimu Woyera mu kupereka uphungu. Chotsiriza, mwachidule mutuwu ufotokozera mitundu, mfundo, ndi zikhalidwe zakaperekedwe ka uphungu ngati Mbusa.

MBUSA NGATI PHUNGU

Khristu akuitana Mbusa aliyense wa Chipentekoste kuti agwire ntchito ya utumwi ya mpingo. Iye wapereka iwo ku mpingo kuti aumbe okhulupirira kukhala ophunzira amphamvu (Aef. 4:11-12). Kuphatikiza kulalikira, kuphunzitsa ndi kutsogolera, Khristu waikiza pa mbusa udindo wakupereka uphungu wa umulungu komanso thandizo ku mamembala omwe akufuna kwathunthu kutsata Khristu.

Mbusa wa Nkhosa za Mulungu

Pamene utumiki Wake umapita ku mapeto, Yesu adalamulira Petro, “Weta nkhosa zanga” (Yohane 21:16). Mu kunena kwake motsanzikana ndi akuluakulu a mpingo wa ku Aefeso, Paulo anatsindika kufunikira kwa abusa kuti, “Tadzichenjerani nokha, ndi gulu lonse pamenepo Mzimu Woyera anakuikani oyanga’anira.” Amayenera “kuweta Mpingo wa Mulungu umene anaugula ndi mwazi wa Iye yekha” (Mach. 20:28). Momwemo, Petro anayitanira akulu a mpingo kuti “Wetani gulu la Mulungu” (1 Pet. 5:2).Amayenera kusamalira opwetekedwa, ovutika, ndi nkhosa zovulala.

Maitanidwe a Mbusa wa Chipentekoste ku uphungu si ntchito yochita kusankha; ndi kuitanidwa kochokera kumwamba. Pamene mamembala a mu mpingo (ndipo nthawi zina, anthu ena) avutika ndi maimvaimva, maubale, ndi nkhani zina za uzimu, athe kukwanitsa kupita kwa Mbusa wao kuti athandizidwe. Monga Mbusa adyetsa, kutsogolera, ndi kuteteza nkhosa, Mbusa wa chipentekoste asamalire iwo amene Khristu waika kuti awatsogolere.

Ubale Wapaderadera

Pakufanizira ndi ogwira ntchito ena owona za thanzi la m'malingaliro, utumiki wakupereka uphungu wa Mbusa ndiwapadera. Anthu nthawi zambiri amapatsa ulemu Mbusa ngati woimira Mulungu. Amaona iwo monga odzozedwa ndi kuyenerezedwa mu ndondomeko ya machiritso. Mosiyana ndi ena owona za thanzi la mu ubongo, cholinga cha Mbusa ndikuti awone anthu a Mulungu "Akukula m'chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu; kwa Iye kukhale ulemerero" (2 Pet. 3:18).

Kuphatikiza apo, abusa amakhala ndi ubale wodalilika umene wakhazikika ndi mamembala awo. Iwo ndi opezeka m'madera onse a miyoyo yao, kuphatikizapo kulira kwao, nkhondo zao, ndinso zokwaniritsa zao. Amayitanidwa kukadalitsa ukwati, kudalitsa ana, ndi kumaliro. Chifukwa cha ubale wapadera otere, mamembala atha kugawana mosavuta kusweka mtima kwao ndi Mbusa wao popanda mantha kapena kukanidwa.

Kuonjezera apo, abusa amapezedwa mosavuta kusiyana ndi anthu ogwira ntchito zoona thanzi la m'malingaliro. Madera ambiri mulibe akatswiri opereka uphungu. Ngakhale atakhala nao, kutumikira kwao anthu sangakwanitse. Chiyembekezo chokhacho cha anthu ndi Mbusa. Komanso, monga Mbuye wao, abusa amagwidwa m'mtima ndi chisoni chifukwa cha "Okambululudwa ndi omwazikana" (Mat. 9:36). Amaona uphungu ngati mwayi ogawa chikondi cha Mulungu ndi iwo opwetekedwa.

Uphungu wa Mbusa

Kudutsa Afirika yonse, njira zingapo zoperekera uphungu zikugwiritsidwa ntchito. Njira iliyonse ndiyofuna kuthana ndikhalidwe lovuta la nyengo za munthu. Komanso iliyonse imaonedwa kutengera kaonedwe kena ka dziko lonse ndi ndondomeko ya chikhulupiriro. Izi zikuphatikizapo, mwa zina, maonedwe achikunja, maonedwe a chikhalidwe cha mu Afirika, ndi kaonedwe ka dziko ka Chikhristu.

Uphungu wa chikunja okhudza m'malingaliro ndi wa zasayansi m'maonedwe ake ndipo nthawi zambiri umakana choonadi cha malemba. Njira iyi imagwiritsa ntchito njira zambiri ndi mankhwala kuti achize ubongo, maimvaimva, komanso kusokonekera kwa chikhalidwe. M'maiko ena mu Afirika, njira zakuchiritsazachikhalidwe zimazindikilidwa ndikuloredwa kuti zigwire ntchito pambali pa njira za ku ulaya zamakhwala. Njira zachikhalidwe izi zimachokera ku

kaonedwe ka mu Afirika komwe amafotokozera moyo ndi ubwino ku mphamvu za uzimu zosaoneka.

Njira yoperekera uphungu ya Mbusa wa Chipentekoste ndiyosiyana ndi maonedwe achikunja kapena njira yachikhalidwe cha Afirika. Njira ya Mbusa wa Chipentekoste ndi yochokera m'Baibulo, yokhazikika pa Khristu, komanso yotsogozedwa ndi Mzimu. Uphungu wa Mbusa ndi wozikika mu ulamuliro wa malemba. Umagwiritsitsa Baibulo ngati Mau a Mulungu ndikuti "Lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo (2 Tim. 3:16). Ngati mau a Mulungu, Baibulo liri ndi mayankho ku zovuta za moyo.

MAZIKO A BAIBULO PA UPHUNGU WA MBUSA

Mbusa wa Chipentekoste amakhulupirira kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu ovumbulitsidwa. Choncho, ndi mlozo wokhazikikapakupereka uphungu. Kuposa chida choyezera chilichonse, Baibulo limabweretsa poyera zinsinsi za mtima wa munthu (Aheb. 4:12). Limathana ndi maziko a kusweka kwa munthu, ndikumuonetsera Yesu Khristu ngati yankho ku mavuto a munthu.

Izi zikutanthauza kuti, monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuzichulukitsa nokha m'choonadi chopezeka m'mau a Mulungu. Kupitilira apo lolani zoonadi izi kukutsogolerani mu utumiki wanu wakupereka uphungu. Ngati mwasakha kubwerekera maganizo a chikunja, muonetsetse kuti maganizowo ali ogwirizana ndi Baibulo komanso zikhalidwe za chikhristu.[1]

Atsogoleri a Chipangano Chakale

Chipangano Chakale chili ndi zitsanzo za atsogoleri ambiri kupereka uphungu wa umulungu. Mwachitsanzo, Mose amataya nthawi yambiri kuweruza ndi kupereka uphungu kwa anthu a Mulungu. Nthawi zina, amapereka uphungu m'magulu. Nthawi zina, amapereka uphungu kwa anthu awiri kapena mmodzi pa nthawi yake. (Eks. 18:13-27). Komabe, nthawi inafika yomwe Mose mwini amafunika uphungu. Mpongozi wake, Yetero, anazindikira kuti iye anali olemedwa kwambiri ndi ntchito yake. Choncho anampatsa uphungu Mose kuti

[1] Pa zambiri zokhudza ubale wa Mbusa wa Chipentekoste ndi Baibulo, onani Mutu 9: "Amakhulupirira Baibulo."

asankhe amuna othekera kuti amuthandize iye. Mose anatsatira uphungu wa Yetero ndipo ntchito inapita patsogolo.

Davide ndi chitsanzo china cha uphungu wa umulungu.Anapereka uphungu kwa anthu ake m'Masalimo. Kumeneko anapereka njira zapamwamba za kuthana ndi mavuto a moyo. Zomwezo zitha kuyankhulidwa kwa Solomo mu Miyambo komanso aneneri ndi zolemba zao.

Utumiki wa Yesu

Yesu mwini anali phungu. Yesaya akumutcha "Wodabwitsa Wauphungu" (Yes. 9:6). Iye nthawi zambiri amapereka uphungu kwa iwo akuvutitsidwa ndi mavuto a za uzimu. Zitsanzo zitatu zodziwika bwino ndi Nikodemo (Yohane 3:1-21), Zakeyu (Luka 19:1-9), ndi mzimayi ogwida m'chigololo (Yohane 8:1-11). Yesu adalengeza "Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wochuluka" (Yohane 10:10).

Nthawi zina, Yesu adatumikira kwa iwo amene adavutika mmalingaliro. Pamene Maria ndi Marita adataya m'bale wawo Lazaro, Yesu anadza kwa iwo. Adaonetsa kumva chisoni ndipo adayenda nao m' kulira kwao (Yohane 11:17-44). Usiku omaliza asanapachikidwe, Yesu, anakhala ndi ophunzira Ake nthawi yambiri kuwakonzekeretsa ku zomwe zichitike. (Yohane 14-16).

Utumiki wakupereka uphungu wa Yesu unakhudza anthu a mitundu yonse. Unakhudza ophunzira, osaphunzira, malo abwino ndi a wamba, olemera ndi osauka, amuna, amayi, ndi ana. Chikondi cha Yesu pa anthu chipangitsa Iye kudutsa zonse zachuma, ubale, ndi zikhalidwe zotchinga kuti akwaniritse ntchito yake yakufuna ndi kupulumutsa otaika (Luka 19:10).

Utumiki wa Paulo

Zigawo zina za makalata a Paulo zitha kuwerengedwa ngatimagawo a uphungu. Zimaonetsera kukhudzidwa kwa ubusa wa mtumwiyu pa anthu a Mulungu. Mkati mwake, akulangiza iwo amene akhudzidwa ndi zovuta za moyo. Mwachitsanzo, analemba kwa okhulupirira a ku Afilipi, "Musadere nkhawa konse." Ngati iwo angapemphere, akumana ndi mtendere wa Mulungu (Afilipi 4:6-7). Chitsanzo china cha utumiki wakupereka uphungu wa Paulo ndi mmene anabwera limodzi ndi ophunzira wake Timoteo kuti amuthandizire mukuthana ndi kusazidalira kwake ndi mavuto akudzionera pansi (2 Tim. 1:3-14; 2:15).

Mu kalata yake ku Akhristu a ku Korinto, mtumwiyu adalakhula za zithu zina malingaliro ndi zikhalidwe zomwe zimaopseza kuononga mpingo kumeneko. M'kalata yake kwa Filemoni, Paulo akufuna kukonza ubale osweka pakati pa Filemoni ndi kapolo wake amene anamuthawa, Onesimo, amene anali tsopano m'bale m'chikhristu. Tsatanetsatane wa makalata a Paulo akuonetsera kuti njira zake pakupereka uphungu zinakhazikika mwa Khristu, kutsogozedwa ndi Mzimu, kulangiza, kuthandiza, kuyanjanitsa, ndi nthawi zina kudzudzula.

NTCHITO YA MZIMU WOYERA MU UPHUNGU

Ngati Mbusa wa chipentekoste, muli wolimbitsana naye mu ntchito ya kupereka uphungu. Wolimbitsana nayeyu ndi Mzimu Woyera. Musalephere kudalira Iye. Taganizira m'silikali amene akupita ku nkhondo wopanda chida chake. Atha kumadziwamalamulo onse akamenyedwe ndi njira za nkhondo, koma popanda chida chake, zotsatila zikhala kuwonongeka. Ndi chimodzimodzi nkupusa kuti Mbusa wa Chipentekoste kulowa mu nkhondo ya uzimu popanda mphamvu ya Mzimu Woyera.

Wothandizira

Kanayi konse Yesu akunena za Mzimu Woyera ngati *Paraclete,* kutanthauza "Wothandizira" kapena "Phungu" mu Chigiriki (Yohane 14:16, 26; 15:26; 16:7). Ngati Phungu wathu wochokera kumwamba, ali wokonzeka kuti atithandize ife mkuyenda kwanthu mu ulendo wopereka uphungu. Ngati angayitanidwe, atsogolera, alimbikitsa, ndi kuthandiza wopereka uphungu. Athandizanso wopatsidwa uphungu kuti athane ndi zovuta ndi ululu wake. (Yohane 14:1; 16:8).

Kupereka uphungu nthawi zambiri pamakhala nkhondo ya uzimu (Aef. 6:12). Ndi Mzimu wa Mulungu yekha amene ali ndi mphamvu zokwanira kuti "Amange osweka mtima" ndi "Ndikulalikira a msinga mamasulidwe" (Yes. 61:1; fanizilani Luka 4:17-18). Baibulo choncho limatilimbikitsa ife kuti "Tidzilimbika mwa Ambuye ndi m'kulimba kwa mphamvu yake" (Aef. 6:10).

Moona mtima, pemphero lodzala ndi chikhulupiriro ndi mbali yofunika mundondomeko yakupereka uphungu. Mzimu Woyera amathandiza mu dera limeneli. Baibulo limati, "Ndipo momwemo Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti chimene tizipempha monga chiyenera, sitidziwa, koma Mzimu mwini atipempherera ndi zobuula zosatheka kunena" (Arom. 8:26). Yesu adati Atate

wakumwamba adzapereka Mzimu Woyera kwa wina aliyense amene amfunsa (Luka 11:9-10, 13).[2]

Yesu ndi chitsanzo chabwino kwa Mbusa wa Chipentekoste. Baibulo limati Iye anadzozedwa ndi Mzimu kuti "Akachiritse onse osautsidwa ndi mdierekezi " (Mach. 10:38). Kudzera mu kudzoza kwake, adalengeza uthenga wabwino kwa osauka, kulalikila am'nsinga mamasulidwe ndikutululutsa ndi ufulu ophwanyika (Luka 4:18). Paulo ndi chitsanzo china chabwino kwa phungu wa Chipentekoste. Kupatula maphunziro ake akulu ndi zomwe anakwaniritsa, anadalira pa mphamvu ya Mzimu Woyera. (1 Ako. 2:4-5). Momwemo, Mbusa wa Chipentekoste amafunikira thandizo la Mzimu Woyera kuti akhale phungu wabwino.

Wowulula Choonadi

Yesu anapitiriza kuphunzitsa kuti Mzimu Woyera ndi wowulula choonadi (Yohane 16:13). Iye adzatithandiza kuti timvetsetse ndikumasulira Mau a Mulungu. Adazaperekanso kuzindikira mu malingaliro a Mulungu ndi malingaliro a anthu amene tikuwapatsa uphungu (1 Ako. 2:11-12). Izi ndi zofunikira chifukwa khalidwe la munthu limadziwika ndi malingaliro ake komanso ndi kufotokozera komwe amakuika pa zochitika za moyo. Munthu amene amakhulupirira kuti matsoka amene azungulira moyo wake alipo chifukwa cha mphamvu zoipa ndi mkwiyo wa makolo amachita molingana ndi izo. Mzimu Woyera athandiza iwo kuti adziwe choonadi chomwe chiwamasule (Yohane 8:32).

Wopereka Mphatso

Mavuto okhudza ubongo ndi osiyanasiyana, ovuta, komanso omangidwa mu chikhalidwe. Zimaphatikizapo zithu za kuthupikomanso uzimu. Choncho, Mphatso za Mzimu Woyera ndi zofunikira pa nthawi yopereka uphungu (1 Ako. 12:8-10). Kudzera mu mphatso zavumbulutso, Mzimu Woyera atha kuperekakuzindikira kwa phungu wa Chipentekoste mu zosoweka za iye akupatsidwa uphungu. Kudzera mu mphatso za Kuzindikira mizimu, Mzimu Woyera atha kuulula kupezeka ndi machitachita a mizimu yoipa. Ndipo, kudzera mu mphatso ya uneneri, phungu atha kuyankhula mau a chiyembekezo ndi machiritso. Mbusa wa Chipentekoste, choncho, ayenera kukhala odzalabe ndi

[2] Pa zambiri zokhudza kuthandiza okhulupirira kulandira Mzimu Woyera, onani Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira Mu ubatizo wa Mzimu."

Mzimu Woyera ndi watcheru kumachitachita Ake mkatikati mwa nthawi yopereka uphungu.[3]

MITUNDU YA UPHUNGU WA ABUSA

Mbusa wa Chipentekoste akhale wokonzeka kuti apereke mitundu ya uphungu yotsatirayi:

Uphungu wa Uzimu

Uphungu wa uzimu umalunjika pa olandira uphungu, ubale wake ndi Mulungu ndi chifuniro cha Mulungu pa moyo wake. Apa, Mbusa wa Chipentekoste, chomwe akukhudzidwa nacho ndikuti wopatsidwa uphunguyo abweretsedwe ku ubale wa moyo ndi Khristu. China chomukhudza ndikuti ubalewo ukhale wathanzi ndi kukula. Zina zokhudza uphungu zikuphatikizapo zotsatilazi:

- Kumvetsetsa kwa munthuyo pa Mulungu ngati okonda, komanso osamalira
- Kumvetsetsa kwa munthuyo pa tanthauzo loona ndi chikhalidwe cha chipulumutso
- Mayendedwe a munthuyo ndi Khristu
- Kumasulidwa ku m'nsinga ndi kuchiritsa kwa mkati
- Kuyanjanitsa zikhalidwe za Chikhristu ku mayendedwe a tsiku ndi tsiku.

M'maonedwe a Chifirika, phungu atha kufuna kuthana ndi m'chitidwe wa wopatsidwa uphungu kufuna kubweretsa machitachita a Chisilamu kapena zikhulupiriro za mizimu ku mayendedwe a Chikhristu. Machitachita awa atha kuphatikizapo kugwiritsa ntchito zithumwa kuonetsetsa kuti ndiwotetezedwa ku mphamvu zoipa ndi matemberero.

[3] Pa zambiri zokhudza mphatso za uzimu, onani Zowonjezera 2: "Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

Uphungu wa pa Ukwati ndi pa Banja

Uphungu wa pa Ukwati ndi pa Banja cholinga chake ndi kupititsa patsogolo zikhalidwe za Chikhristu ndi kukhala kwa umulungu mu mabanja a mamembala. Mtundu wa uphungu uwu utha kuphatikizapo kupereka uphungu munthu payekha kapena gulu pa msonkhano. Zikuphatikizapo zotsatilazi:

- Uphungu wa iwo omwe sanakwatirane koma akukonzekera akulowa mchimangiriro chaukwati.
- Uphungu owonjezera kwa iwo omwe ali mu ukwati ndipo akufuna kuzamitsa ubwenzi wa wina ndi mzake.
- Uphungu ku ma ukwati omwe akukumana ndi zovuta mu ukwati wawo.
- Uphungu ku makolo a Chikhristu
- Uphungu ku gulu la banja kuti athandize mamembala ao omwe akuvutika ndi maubale pakati pao.
- Uphungu okhudza miyambo ya banja monga ukwati, kubadwa kwa mwana, imfa, ndi maliro.

Uphungu pa Mavuto ndi pa Kuthandizira

Uphungu woperekedwa pa mavuto ndi pa kuthandizira umalunjika pakuthandiza anthu okhudzidwa ndizowachitikira za moyo zoopsa. Zochitikazi zikuphatikizapo zotsatilazi:

- Kudwala kwa kanthawi kapena imfa ya okondedwa wao.
- Chilala, njala, mliri, zovuta za nyengo.
- Wovulazidwa ku upandu kapena nkhanza.
- Kusalembedwa ntchito ndi umphawi.

Mu nthawi ya zovutayi, mamembala atha kufuna munthu wina amene angawamve pamene akugwira ntchito mu ululu wao. Ngati Mbusa, siwokonzeka kuti athane ndi nyengo zopereka chiopsezochi ngati kudzipha, ndi kukhumudwa, iye ayenera kulozera osautsidwayo ku phungu woyenerezedwa.

Uphungu Mukukula

Uphungu mukukula umalunjika pa kupatsa mphamvu anthu kuti apambane m'moyo. Cholinga chake ndikuwathandizira iwo kuti asankhe njira yabwino chitsogolo. Masalimo ndi Miyambo amapereka mau ambiri a nzeru ndi uphungu (Chitsanzo, Mas. 32:8; Miy. 15:22).

MFUNDO ZA UPHUNGU

Kufufuza koganiza bwino zokhudza m'kumano wa Yesu ndi mkazi wa ku Samariya mu Yohane 4 zikuvumbulutsa mfundo zinai za uphungu zofunika zomwe Mbusa wa Chipentekoste atha kufuna kuti agwiritse ntchito:

Kukhazikitsa Chikhulupiriro

Yesu adayamba ndondomeko ya kupereka uphungupakukhazikitsa chikhulupiriro pakati pa Iye mwini ndi mkaziyo. Iye adaonetsera ulemu wosamuweruza mkaziyo ndikusonyeza chikondi komanso kumulandira kopanda malire. Anapitiriza kufikira iye pakudutsa zotchinga za chikhalidwe zomwe zinalipo (Yohane 4:7-9, 17-18).

Kumvetsera mwa Chidwi

Yesu adafunitsitsa kuti apeze chizindikiro cha nyengo ya mkaziyo pakufunsa mafunso ofufuza. Kenako adamvetsera mwatcheru kuzomwe iye anene ndikuyankha moyenera. Mayankho Ake analankhula za kumvetsetsa kwake kwakuya pa zinthu za uzimu zomwe mkaziyo anasowekera. Yesu adapitilira kutsutsa timadontho takhungu m'malingaliro ake zomwe zimatchinga iye kuti avomereze choonadi ndikupeza ufulu mwa Khristu. (Yohane 4:9-16, 21-24).

Kuyankhula Choonadi M'chikondi

Pamene panali poyenera kutero, Yesu mwachikondi anatsutsa bodza la mkaziyo ndikugwiritsa ntchito choonadi (Yohane 4:16-18; Aef. 4:15).

Kukhala Osasuthika

Munthawi yonse, Yesu adakhalabe pachindunji pa cholinga Chake chothandiza mkaziyo kuti azindikire cholinga chake chenicheni pakukhala ndi moyo (Yohane 4:10, 13-14, 16-18, 21-24). Mkaziyo adavomereza machimo ake ndikumuzindikira Iye ngati Mesiya. Kenako iye anathamanga kukawauza ena za Iye (Yohane 4:28-29).

MAKHALIDWE PA UPHUNGU

Ngati oyimira Khristu, komanso osamalira anthu ake, abusa a Chipentekoste ayenera kukhala amuna ndi akazi angwiro. Muyenera kuganizira zikhalidwe zotsatilazi pamene mukupereka uphungu. Kutsatira mfundozi mudzateteza inu pamodzi ndi wolandira uphungu:

Zindikilani Malire Anu

Muyenera kukhala oona mtima pa zokhudza kuthekera kwanu ndi malire anu mu uphungu, ndipo musayesere kuyenda mopitilira malirewo. M'maiko ena, akatswiri a uphungu amafunikira kuti anthu atsimikizire.

Kulozera

Muyenera kudziwa pamene mwafika pa malire anu. Ngati simunaphunzitsidwe kapena kuyenerezedwa kuti mupereke uphungu m'madera ena, konzekani kulozera ma membala anu ku aphungu a Chikhristu otsimikizika. Muyeneranso kukhala okonzeka kulozera pamene ubwenzi womangodalira wakula, kapena pamene wolandira uphungu sakupindulanso kuchokera ku uphungu wanu.

Ungwiro pa Zachiwerewere/Zogonana

Ngati Mbusa, muyenera kukhala osamalitsa pamene mukupereka uphungu kwa mkazi kapena mwamuna. Ngati kukopeka kwa m'maimvaimva kwayamba kuchitika pakati pa inu ndi wolandila uphungu, magawo akupatsana uphungu aimitsidwe ndipo munthuyo alozeredwe kwa phungu wina.

Chinsinsi

Uthenga womwe waperekedwa mu chinsinsi ulemekezedwe komanso usakambidwe ndi anthu ena.

Ngati Mbusa wa Chipentekoste, musanyalanyaze udindo wanu kutumikira ngati phungu kwa anthu a Mulungu. Koma, Yesu Khristu ngati chitsanzo chanu, ndi mzimu Woyera ngati mthandizi wanu, muyenera kugwiritsitsa mwa chidwi utumiki ofunikawu.

~ Mutu 27 ~

Kuteteza Nkhosa

Mu mbiri yonse, atsogoleri oyipa, achita zoipa zosasimbika kwa anthu. Zoipa za upanduzi zikuphatikizapo kuphana, kupulula fuko, ndi nkhondo zopanda chilungamo. Ena ndi olakwa pakuchita m'chitidwe wankhazawu; ena ndi olakwa pakungoyang'anira osachitapo kanthu kuimitsa iwo. Mokhumudwitsa, Afirika alinso ndi gawo lake ku zoipazi. Lamulo lodziwikiratu ndilakuti dziko lililonse lasenza udindo wakuteteza anthu ake kuchokera kwa anthu ochita zoipa. Chomwecho chili choonadi chokhudza Mpingo. Mpingo uli ndi udindo wakusamalira anthu ake kuchokera ku kuukira kwa Satana ndi khamu lake la ziwanda.

Yesu adachenjeza za aneneri onyenga, amene Iye adati, "Amene adza kwa inu ndi zovala za nkhosa, koma m'kati mwao ali afisi olusa." Adawalangiza, "Mudzawazindikira ndi zipatso zao" (Mat.7:15-16). Paulo akuperekanso chenjezo lofanana nalo ku Akulu a ku Aefeso. Adawauza, "Idzalowa mimbulu yosautsa, yosalekerera gululo. Ndipo mwa inu nokha adzauka anthu, olankhula zokhotakhota, kupatutsa ophunzira awatsate. Chifukwa chake chilimikani!" (Machitidwe 20:29-31).

Mutu uwu ukamba za udindo wodziwikiratu wa Mbusa wa Chipentekoste wa kulondera nkhosa za Mulungu kutsutsana ndi atumiki awa a Satana. Uyankha mafunso oti: Kodi Baibulo limati chiyani zokhudza udindo wa Mbusa wa

Chipentekoste pakuteteza nkhosa?" komanso "Kodi iye apange chiyani kuti akwaniritse udindowu?"

KHALIDWE NDI KUFUNIKIRA KWA NKHOSA

Baibulo limagwiritsa ntchito chithunzithunzi cha Mbusa ndi nkhosa kuti lifotokozere ubwenzi pakati pa Mbusa ndi anthu ake. Kuti timvetsetse bwino udindo wa Mbusa wa Chipentekoste ku mpingo wao, afunikira kumvetsetsa khalidwe ndi mtengo wa nkhosa.

Khalidwe la Nkhosa

Mbusa wina kamodzi anadandaula, "Kutsogolera anthu anga ndi ngati kuweta amphaka!" Kuweta amphaka nkosatheka. Amakhala a mwano ndipo amakana kupita komwe ukuwatsogolera. Koma sichoncho ndi nkhosa. Nkhosa zimagonjera. Ndi zokonzeka kutsatira Mbusa komwe atsogolere. Izi ndi zabwino. Komabe, chikhalidwe chotere chimaika nkhosa pa chiopsezo. Zimatha nthawi zina mopusa kutsata munthu wolakwika. Choncho zikufunikira chisamaliro ndi kutetezedwa.

Akhristu enieni amagonjera okha ku Mbusa Wabwino. Iwo ndiwokonzeka kumutsatira Iye kulikonse awatsogolere (Yohane 10:27). Komabe, Akhristu ena ndi osakhwima, ndipo monga nkhosa amasokoneza a nkhandwe auzimu ndi abusa enieni. Mwakhungu amatsatira amuna kapena akazi a Mulungu omwe ndi abodza.

Kupitirira apo, nkhosa zilibe kudziteteza kwaokha kwa chilengedwe. Pachifukwa ichi, zitha kuvulazidwa ndipo zisowekera Mbusa kuziteteza. Komanso zimakonda kuyendayenda kuchoka pachitetezo cha khamu la nkhosa ndi chisamaliro cha mbusa. Pamene izi zachitika, zimakhala nyama zosavuta kuphedwa ndi nyama zolusa. Ichi ndi choonadinso pa Akhristu ambiri. Amakonda kuyendayenda kuchoka pachisamaliro cha Mbusa wao ndi pachitetezo cha mpingo. Amafunikira chisamaliro ndi chitetezo cha Mbusa owona.

Kufunikira kwa Nkhosa

Mu nthawi za Baibulo, nkhosa zinali za mtengo wache. Nthawi zambiri Zinali gwero la moyo wa mabanja. Zimapereka nyama pa chakudya, mkaka pakumwa, ubweya pazovala, ndi zikopa zake kukokonzera pokhala ndi zolinga zina. Akhristu ali a mtengo wake kukufunikira kwao kwa Mbusa Wamkulu. Izi ndi zoona ku zifukwa zosachepera ziwiri:

Choyamba, Akhristu ali ofunikira kwa Khristu chifukwa cha mtengo wa ukulu omwe Iye analipirira chifukwa cha chiombolo chao. Yesu mwini adanena, "Ine ndine Mbusa Wabwino; mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha nkhosa" (Yohane 10:11). Petro akutikumbutsa za kufunikira kwathu kwa Khristu: "Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zobvunda, golidi ndi siliva…koma ndi mwazi wa mtengo wake wapatali" (1 Pet. 1:18-19).

Koposa, Akhristu ndi ofunikira kwa Khristu chifukwa cha ubale wao wapaderadera ndi Iye. Kale adali "Opanda Khristu, alendo a padera ndi mbumba ya Israele, ndi alendo alibe kanthu ndi mapangano a malonjezano, opanda chiyembekezo, ndi opanda Mulungu m'dziko lapansi." Koma iwo tsopano "anakusendezani mukhale chifupi m'mwazi wa Khristu" (Aef. 2:12-13). Petroatikumbutsa kuti anthu a Mulungu ndi "Mbadwa yosankhika ansembe achifumu, mtundu woyera mtima, anthu a mwini wache" (1 Pet. 2:9). Monga nkhosa zosankhika za Mulungu, anthu Ake ndiwoyenera chisamaliro chapadera.

ZIOPSEZO ZOLIMBANA NDI NKHOSA

Ngati Mbusa wa Chipentekoste okhulupirira, muyenera kukhala tcheru kuti muteteze anthu anu ku chiopsezo chochokera ku aneneri abodza ndi aphunzitsi abodza.

Kuzindikira Aneneri Abodza ndi Aphunzitsi Abodza

Mneneri wabodza ndi aliyense amene amadzinenera kutiakuyankhulira Mulungu, koma, mu zenizeni, amayankhula mu dzina la iwo eni kapena mu dzina la kamulungu kabodza kapena mzimu woipa (Yer. 23:16). Baibulo limatichenjeza kuti Mulungu amatsutsana ndi aneneri onama otere pakati pa anthu a Mulungu (Ezek. 13:9). Yesu anachenjeza kuti aneneri onama nthawi zina amatha "Kuonetsa zizindikiro zazikulu ndi zozizwa" ndipo kuti zimaopseza "Kuti akanyenge, ngati nkotheka, osankhidwa omwe" (Mat. 24:24). Paulo akuwatcha iwo "Mimbulu yosautsa" amene "Olankhula zokhotakhota, kupatutsa ophunzira awatsate" (Mach. 20:29-30). Iye adalembanso kuti amaphunzitsa nthano ndikunena zomwe anthu akufuna kuti amve (2 Tim. 4:3-4).

Aphunzitsi abodza ali mofananira ku aneneri abodza. Pamene m'neneri wabodza amayesezera kuyankhulira Mulungu, mphunzitsi wa bodza mosasamala amapotoza Mau a Mulungu kunena zinthu zina kusiyana ndi zomwe zimatanthauza. Nthawi zambiri amachita izi kuti apeze cholowa kwa iwo eni (Tito

1:11). Baibulo limanena kuti anthu amenewa ali osaphunzira ndi osakhazikika ndikuti amapotoza Malemba ndikuzionong a iwo eni (2 Pet. 3:16).

Pali njira ziwiri zomwe tingathe kuzindikira aneneri abodza ndi aphunzitsi abodza mu mpingo lero lino:

1. Pakuyang'anira miyoyo yao. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake, "Yang'anirani mupewe aneneri onyenga, adza kwa inu ndi zobvala za nkhosa, koma m'kati mwao ali afisi olusa. Mudzawazindikira ndi zipatso zao" (Mat. 7:15-16). Amayesera kukhala chinthu chomwe iwo saali. Amavala ndi kukhala ngati oyera mtima; amagwiritsa ntchito njira zatsopano za chipembedzo, ndipo amapemphera mapemphero osangalatsa. Ena amathanso kuchita zozizwa zazikulu. Kunja, amaoneka ngati oyera ndi odzozedwa. Komabe, mkati mwawo iwo ndi olanda, onama, ndi a chigololo. Chipatso cha moyo wao wanseri chimavumbulutsa chinyengo chawo. Palibe mwamuna kapena mzimayi amene amakhala moyo wopanda umulungu amene ali m'neneri owona wa Mulungu.

Yesu adawatsutsa aphunzitsi abodza a m'nthawi yake: "Tsoka inu… onyenga! Chifukwa mufanafana ndi manda opanda njereza, aonekera okoma kunja kwake, koma adzala m'katimo ndi mafupa a anthu akufa ndi zonyasa zonse…inunso muonekera olungama pamaso pa anthu, koma m'kati muli odzala ndi chinyengo ndi kusaweruzika" (Mat. 23:27-28). Amuna ndi amayi owukira chotere amakana kudzipereka okha ku ulamuliro wa Mulungu ndi Mpingo.

2. Pakuzindikira njira zao ndi zolinga zao. Njira ya chiwiri yomwe tingazindikire aneneri onama ndi aphunzitsi abodza mu mpingo ndipakuzindikira zolinga zao ndi njira zao. Njira yodziwikiratu mneneri wonama ndikupititsa patsogolo zokhumba za iwo eni. Kuti achite izi, amakhotetsa mokondwera Mau a Mulungu. Nthawi zambiri amatenga ndime za Baibulo molakwika ndi kuzitanthauzira kuti zifanizidwe ndi zomwe akukhumba. Cholinga chao ndi"Kupatutsa gululo kuti awatsate" (Mach. 20:30). Amakhudzidwamochepa ndi owatsatira awo pa zokhudza chipulumutso kapena kukula mwa Khristu. Iwo amakhudzidwa ndi zomwe angapeze komanso ulemerero wa iwo eni.

Ziphunzitso Zabodza mu Afirika

Mwachisoni, mipingo ya Chipentekoste yambiri mu Afirika, ziphunzitso zabodza ndi ma uneneri abodza zikukhala zochitika za tsiku ndi tsiku. Ziphunzitso zimenezi zimalonjeza dalitso kwinaku zikukana kufunikira kwa chikhulupiriro chodzipereka ndi kulapa ku uchimo. Kulunjika kwambiri pa zokhumba za anthu

za kanthawi kochepa, amanyalanyaza kukula kwao kwa uzimu komanso kukula mu chisomo. Mu kupanga izi, amalephera kubweretsa otayika kwa Khristu komanso kukonzekeretsa oyera mtima ku moyo wosatha (Marko 8:36). Baibulo limachenjeza mwa mphamvu kutsutsana ndi ziphunzitso zotere (1 Tim. 4:1).

Ziphunzitso ziwiri zabodza zomwe ndizofala mu Afirika:

1. Uthenga wakulemera. Chiphunzitso choyamba cha izi ndi chotchedwa "Uthenga wakulemera." Uthenga wakulemera ndi chiphunzitso chakuti okhulupirira onse ali ndi ufulu wa pangano ku madalitso a thanzi, chuma, ndi kulemera. Madalitso amenewa atha kupezeka kudzera m'chikhulupiriro, kuvomereza kwabwino, ndi mwa kudzala "mbeu ya chikhulupiriro."

Pamene zili zoona kuti Mulungu amadalitsa iwo amene mokhulupirika amamutsata Iye, uthenga wakulemera si uthenga womwe Yesu ndi atumwi adaulalikira. Yesu adalamulira anthu, "Tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino" (Marko 1:15). Petro analengeza, "Chifukwa chake lapani, bwererani, kuti afafanizidwe machimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zochokera kunkhope ya Ambuye" (Mach. 3:19). Paulo akuchenjeza, "Nthawi zakusadziwako tsono Mulungu analekerera; koma tsopanotu ali kulamulira anthu onse ponseponse atembenuke mtima" (Mach. 17:30).

Mpingo weni weni wa Chipentekoste ukane uthenga wa kulemera chifukwa ndi odzikonda osati okhazikika pa Khristu. Umalunjika pa zokhumba za kuthupi za wanthu osati pantchito ya kuombola ya Mulungu. Uthenga wakulemera umatsindika pa kudalitsika osati kutumikira. Ndi uthenga okhotakhota omwe uli ndi zotsatira zowononga pa Akhristu. Chenjezo la Paulo kwa Akhristu a ku Agalatiya likugwira: "Ndizizwa kuti msanga motere mulikupatuka kwa Iye amene anakuitanani m'chisomo cha Khristu, kutsata Uthenga Wabwino wina, umene suli wina.…koma ngakhale ife, kapena mngelo wochokera Kumwamba, ngati akakulalikireni Uthenga Wabwino osati umene tidakulalikirani ife, akhale otembereredwa!" (Agalatiya 1:6-8).

2. Kusakaniza. M'chitidwe owononga m'mipingo ya Chipentekoste mu Afirika ndi kusakaniza. Kusakaniza uku ndikusakaniza kwa chikhulupiriro cha Chikhristu ndi zinthu za chipembedzo m'zikhulupiriro zaku Afirika. Aneneri abodza ndi aphunzitsi abodza nthawi zina amagwiritsa ntchito njira zimenezi kuti

akope wanthu ku mipingo yao. Zitsanzo zambiri za kusakaniza uku zitha kupezeka mu Afirika yonse. Ku madzulo a dziko la Afirika, zitsanzo zikuphatikizapo

- Chopereka cha kwa mneneri
- Chopereka choombola
- Chopereka cha nsembe
- Kugulitsa komanso kusagwiritsa ntchito monga mwa malemba mafuta odzozedwa
- Kugulitsa ndi kugwiritsa ntchito madzi oyera
- Kugulitsa ndi kugwiritsa ntchito uchi ndi mkaka
- Kugulitsa zithunzi za "Munthu wa Mulungu"
- Kugwiritsa ntchito tsache loyera (kuti wina asese adani ake)
- Kugwiritsa ntchito thope lochokera ku Nyanja Yakufa
- Kugwiritsa ntchito madzi kuchokera ku Mtsinje wa Yordano
- Kulipira kuti ufunsire pa uneneri.

Zizolowezi izi ndi kuyesera kuti "achititse Chikhristu" miyambo ya zochitika za chipembedzo. Izi zimazungulira pa ndalama ndi lonjezo la dalitso ndi chitetezo pa iwo amene azivomera. Ziyenera kukanidwa ndi kutsutsidwa mu kukonda "uthenga wabwino woona" (Akolose 1:5-6).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, osaiwala konse kuti mwagwiriziza m'manja mwanu tsogolo la muyaya la iwo amene mukuwatumikira. Choncho yang'anitsitsani mosamala zomwe mukuchita ndi kuphunzitsa. Ngati mulephera kuphunzitsa choonadi, ndikudzipereka ku ziphunzitso zabodza, anthu adzasocheretsedwa, mpingo kuwonongeka, ndipo mudzaweruzidwa ndi Mulungu.

Zotsatira za Ziphunzitso ndi Uneneri wa Bodza

Pali njira zisanu zomwe ziphunzitso zabodza zimavulaza mpingo:

1. Ziphunzitso zabodza zimalimbikitsa kusapembedza. Choonadi chimayeretsa ndi kulimbikitsabe Akhristu kukhala moyo wa umulungu (Yohane 17:17). Kumbali ina, ziphunzitso zabodza zimasokoneza malingaliro ndi mtima, ndipo zimalimbikitsa chisembwere (1 Ako. 15:33).

2. Ziphunzitso zabodza zimatulutsa atsogoleri opanda umulungu. Choonadi chimatulutsa atsogoleri otumikira a umulungu; koma, ziphunzitso zabodza zimatulutsa atsogoleri opanda umulungu, ndi wolamulira mwa nkhanza. Mtsogoleri weniweni wa Chikhristu "ayenera kugwira mau okhulupirika monga

mwa chiphunzitso, kuti akakhonze kuchenjeza m'chiphunzitso cholamitsa, ndi kutsutsa otsutsana naye" (Tito 1:9).

3. Ziphunzitso zabodza zimaika anthu mu ukapolo. Choonadi chimamasula anthu (Yohane 8:32). Koma, zosokoneza, zimaika anthu mu ukapolo (Agalatiya 4:9). Paulo anauza Agalatiya, "Khristu anatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; chifukwa chake chirimikani musakodwenso ndi goli la ukapolo" (Agal. 5:1).

4. Ziphunzitso zabodza zimatulutsa Akhristu Ofooka. Akhristu amene aphunzitsidwa ziphunzitso za bodza ndi zosokoneza samakula m'chisomo. Amakhalabe makanda mu uzimu. Ngakhale mpingo utakula m'chiwerengero, chimakhalabe chofooka ndi chosachita kanthu.

5. Ziphunzitso zabodza zimatsogolera ku chiweruzo ndi chiwonongeko. Baibulo limayakhula za "Osaphunzira ndi osakhazikika apotoza, monganso atero nao malembo ena, ndi kuzinonga nao eni" (2 Pet. 3:16).

KUTETEZA NKHOSA

Ngati mbusa wa nkhosa za Mulungu, nthawi ndi nthawi mudziyang'anira nkhosazo. Muyenera kukhala ofuna kuti mupereke moyo wanu chifukwa cha izo (Yohane 10:11; fanizilani 1 Sam. 17:34-35). Nazi njira zisanu, zomwe inu monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuimamo pakuteteza anthu a Mulungu:

Pakupempherera Nkhosa

Choyamba, muyenera nthawi zambiri kugwada pamaso pa Atate m'malo mwa gulu lonse. Mkuchita izi, mudzalandira kwa Iye mphamvu ndi nzeru zomwe musowekera kuti musamalire ndi kuteteza nkhosa. Kuonjezera apo, mapemphero anu adzaonetsetsa kuti mkono wa Mulungu woteteza ukhalebe pa anthu ake.

Pakugwiritsa Ntchito Kuzindikira Kwa Uzimu

Chachiwiri, muyenera kugwiritsa ntchito kuzindikira kwa uzimu. Baibulo lachenjeza za "Mizimu yosocheretsa ndi maphunziro a ziwanda" (1 Tim. 4:1). Muyenera tsono kufunsa Mulungu kuti akupatseni mphatso ya kuzindikira mizimu kuti ikuthandizireni kuvumbulutsa chiphunzitso chilichonse kapena kuonekera kwazinthu za uzimu zomwe sizichokera kwa Mulungu. Mphatso ya uzimu

imeneyi ikupangitsani kuti mudziwe ngati munthu wina mu mpingo akuchita pansi pa kukhudza kwa Mzimu Woyera kapena mzimu wonyansa.[1]

Pakuphunzitsa Chiphunzitso Cholamitsa

Chachitatu, muyenera kuphunzitsa ndi kulalikira chiphunzitso cholamitsa (2 Tim. 4:2; Tito 1:9). M'chitidwe uwu udzalimbikitsa nkhosa ndi kuwateteza iwo ku ziphunzitso zabodza. Zidzawathandizira kuwasunga iwo pa njira ya chiyero (Masalimo 119:9-11).

Pa Kuzindikira Aneneri Abodza ndi Aphunzitsi Abodza

Chachinayi, muyenera kuchenjeza mpingo ku aneneri abodza ndi aphunzitsi abodza. Baibulo likufotokozera za njira zitatu kuti tizindikire nkhandwe zimenezi mu chovala cha nkhosa:

1. Zonenera zao sizimachitika. Ngati ma uneneri sachitika, iwo sanamve kuchokera kwa Mulungu. Ndi aneneri abodza (Yer. 28:9).

2. Amawalozera anthu kunja kwa Choonadi. Ngakhale kuti ma uneneri ao amatha kukwaniritsidwa, ngati awalozere anthu kunja kwa uthenga owonadi wabwino, iwo ali aneneri abodza (Deut. 13:1-3; Agal. 1:6-9).

3. Amakhala Moyo Wopanda Chiyero. Ngakhale ma uneneri ao atakwaniritsidwa, ndipo amachita zizindikiro zodabwitsa, ngati akukhala moyo wosati wa umulungu, iwo ali aneneri abodza (2 Pet. 2:10-15). Yesu akuchenjeza, "Mudzawazindikira ndi zipatso zao" (Mat. 7:15-16; komanso vv. 22-23).

Ngati woyang'nira wokhulupirika, muyenera kuteteza nkhosa kuchokera ku zilombo zolusa, ndipo m'mene Mulungu achitira ndi inu, muyenera kulondolera izo kunjira yolondola (Masalimo 23:3).

Pakuvumbula ziphunzitso Zabodza

Pomaliza, tetezani nkhosa za Mulungu pakuzindikira ndi kukonza ziphunzitso za bodza ndi ma uneneri abodza mu mpingo. Paulo adalemba, "Musanyoze manenero." Komabe, mwachangu adaonjezera, "Yesani zonse; sungani chokomacho, mupewe maonekedwe onse a choipa" (1 At. 5:20-22). Choncho,

[1] Pa zambiri zokhudza mphatso za uzimu, onani Zowonjezera 2:"Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10."

monga mbusa pa nkhosa za Mulungu, mufunikira kuti mukhalebe odziwa za zinthu zomwe zikuphunzitsidwa mu mpingo. Pali njira zitatu zomwe mungathe kuchitira izi:

1. Pakuyang'anira zimene ziri mkuphunzitsidwa. Ziphunzitso zabodza zitha nthawi zina kulowa mu mpingo kudzera m'magulu ang'onoang'ono kapena m'maphunziro a Baibulo. Munthu waulamuliro wa gululo amayamba kuphunzitsa chinthu china chomwe wangochimva kapena kuwerenga. Mu kanthawi kochepa chosocheretsacho chimafalikira mu mpingo wonse. Choncho,muyenera, kuyang'anira mwa pafupi zomwe zikuphunzitsidwa m'makalasi a sukulu ya baibulo, makalasi a ubatizo, m'milaga, mikumano ya nyumba, ndi magulu ena kuti muonetsetse kuti choonadi chikuphunzitsidwa.

2. Pakukhala wozindikira zimene akumamvera. Lero, njira zofalitsira uthenga zadzadza ndi mitundu yonse ya ziphunzitso ndi maulaliki. Anthu akumvetsera amuna ndi akazi amenewa. Pamene ena ambiri olalikira akufalitsa uthenga wabwino okhulupirika, ena akuphunzitsa zolakwika. Muyenera kuzindikira zimene anthu ali kumvetsera kuti muwalozere kuchoonadi cha Mau a Mulungu.

3. Pakukhala "Wosunga chipata." Monga Mbusa, muyenera kuima ngati osunga chipata ku mpingo wanu. Mu njira ina, muyenera kuyang'anira mosamalitsa munthu amene mukumulora kuti alalikire ku mpingo wanu. Mosatengera mlingo wakutchuka kapena mphamvu za mlaliki, ngati alibe chikhalidwe chapamwamba, kapena ngati watembenuka kusiya choonadi, musawalole pa gome lanu.

Mbusa wa Chipentekoste amene ndi wokhulupirika kuteteza nkhosa za Mulungu amabweretsa madalitso mzonse ku mpingo ndi kwa iwo eni. Nkhosa zimasangalala pansi pa chitetezo cha Mbusa wao, ndipo zimakula kukhala ophunzira aKhristu okhwima. Mbusayo amadalitsikanso. Iye adzapatsidwa mphoto ya kukhutitsidwa pakudziwa kuti adakhala mtumiki wabwino ndi wokhulupirika.

Petro adayankhula za mphoto ya woyang'anira wokhulupirika: "Wetani gulu la Mulungu lili mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokakamiza, koma mwa ufulu, kwa Mulungu; osatsata phindu lonyasa, koma mwachangu; osati monga ochita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo. Ndipo pakuonekera Mbusa wamkulu, mudzalandira korona wa ulemerero, wosafota" (1 Pet. 5:2-4).

~ Gawo 7 ~

MBUSA WA CHIPENTEKOSTE NGATI MTSOGOLERI

~ Mutu 28 ~

Utsogoleri wa Chipentekoste

Paulo ndi gulu lake la atumwi anachoka ku Galatiya kulowera cha kumadzulo m'chigawo cha Asiya. Komabe, Mzimu Woyera anawalepheretsa kupitirizabe kuyenda m'njira imeneyo. Choncho, anaganiza zolowera chakumpoto m'chigawo cha Bitiniya. Ndiponso Mzimu anawaletsa. Chotero anatembenukiranso kumadzulo. Kenako anafika ku Troasi, mzinda womwe unali kumpoto chakumadzulo kwa nyanja ya Aegean. Kumeneko kunachitika chinthu chodabwitsa.

Usiku, Mzimu Woyera anaonetsa Paulo masomphenya. M'masomphenyawo, mtumwiyu anaona munthu wa ku Makedoniya ataimirira ndi kuchonderera kuti, "Muolokere ku Makedoniya kuno mudzatithangate ife" (Machitidwe 16:9). Pamene Paulo adagawana masomphenya ake ndi gulu lake, onse adavomelezana kuti adachokera kwa Ambuye. Luka anafotokoza kuti, "Pamene anaona masomphenyawo, pomwepo tinayesa kutulukira kunka kuMakedoniya, poganizira kuti Mulungu anaitanira ife kulalikira Uthenga Wabwino kwa iwo" (ndime 10). (Zitsanzo zina za Paulo akutsogozedwa ndi Mzimu zikupezeka mu Machitidwe 13:1-5; 15:28, ndi 20:22.)

Paulo ndi chitsanzo chabwino cha mtsogoleri wa wachipentekoste. Iye ankatsogolera ena pofuna kuti Mzimu Woyera amutsogolere. Pochita izi, anali kutsatira chitsanzo cha Yesu, amene Iye mwini anatumikira pansi pa kudzozedwa ndi chitsogozo cha Mzimu Woyera (Luka 4:1; Yohane 5:19; Machitidwe 10:38).

Mutu uwu ukambirana za utsogoleri wa Chipentekoste. Udzapereka chitsanzo cha utsogoleri chozikidwa pa njira ya Yesu ndi atumwi. Choyamba, ufotokoza tanthauzo la kukhala mtsogoleri wa Chipentekoste. Kenako, ukambirana za ena mwa makhalidwe ndizochita za enieni a Chipentekoste.

KUFOTOKOZA UTSOGOLERI WA CHIPENTEKOSTE

Ngakhale zili zoona kuti abusa a Chipentekoste amagwiritsa ntchito njira zambiri za utsogoleri monga abusa omwe si a Chipentekoste, pali kusiyana kwakukulu. Kayendetsedwe ka Mbusa wa Chipentekoste pa utsogoleri amaumbidwa kwambiri ndi zochita zake ndi Mzimu. Kumvetsetsa kwawo kwapadera kwa momwe Mzimu amagwirira ntchito m'miyoyo yawo ndi miyoyo ya ena kumakhudza kwambiri momwe amatsogolera.

Mtsogoleri wa Chipentekoste ndi mwamuna kapena mkazi wosankhidwa ndi Mulungu amene anadzazidwa ndi Mzimu ndipo amafunafuna nzeru ndi chitsogozo cha Mzimu. Cholinga chake ndi kusonkhezera gulu linalake la anthu a Mulungu kuti akwaniritse mokhulupirika ndi mogwira mtima udindo wawo woikidwa ndi Mulungu popititsa patsogolo ntchito yake padziko lapansi. Tiyeni tione tanthauzo ili m'zigawo zake zinayi.

Oitanidwa ndi Mulungu

Choyamba, mtsogoleri weniweni wa Chipentekoste waitanidwa ndi Mulungu kuti atsogolere anthu ake. Chifukwa cha zimenezi, iye anagwirizana kwambiri ndi Paulo, amene anadzitcha "kapolo wa Yesu Khristu, mtumwi woitanidwa, wopatulidwa kukanena Uthenga Wabwino wa Mulungu" (Aroma 1:1).

Odzazidwa ndi Mzimu

Kenako, mtsogoleri wa Chipentekoste wadzazidwa ndi Mzimu ndipo amafuna kukhala moyo wake "moyenda ndi Mzimu" (Agalatiya 5:25). Iye amaona mozama lamulo la Khristu lakuti, "koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yochokera Kumwamba" (Luka 24:49), ndi malangizo a Paulo akuti, "mudzale naye Mzimu" (Aefeso 5:18).

Wofunafuna Chitsogozo cha Mulungu

Chachitatu, mtsogoleri wa Chipentekoste amafunafuna chitsogozo cha Mzimu mu zonse zomwe amachita. Amazindikira kuti ntchito yake yayikulu ndi

kuchita chifuniro cha Mulungu monga chawululidwa m'Malemba ndi mwa Mzimu Woyera. Mtsogoleri weniweni wa Chipentekoste ndiye amathera nthawi yochuluka pakusanthula Baibulo ndi kupemphera.

Osonkhezera Anthu a Mulungu

Pomaliza, mtsogoleri wa Chipentekoste amafuna kukopa gulu linalake la anthu a Mulungu – monga Mpingo wadziko lonse kapena wapamalo – kuti akwaniritse mokhulupirika ndi mogwira mtima udindo wawo woikidwa ndi Mulungu popititsa patsogolo utumwi wa Mulungu padziko lapansi.

MAKHALIDWE A MTSOGOLERI WA CHIPENTEKOSTE

Kodi nchiyani chimamuyenereza mwamuna kapena mkazi kukhala mtsogoleri wa Chipentekoste? Ngati pongoyambira chabe, mtsogoleri weniweni wa Chipentekoste ayenera kubadwa mwa Mzimu, kudzazidwa ndi Mzimu, ndi kutha kutsogolera mu kuyenda mwa mphamvu ya Mzimu. Ayenera kuzindikira mawu a Mzimu ndi kukhala waluso mu utumiki wa mphatso zauzimu. Ayenera kumvetsetsa ndi kudzipereka ku utumwi wa Mulungu. Ndipo ayenera kukhala okonzeka kupereka moyo wake chifukwa cha Khristu, ngati nsembe yoteroyo ingafunike.

Monga mtsogoleri wa Chipentekoste, moyo wanu ndi utumiki wanu uyenera kuzindikirika ndi makhalidwe asanu ndi amodzi ofunikirawa:

Umphumphu

Koposa zonse, muyenera kuyetsetsa kukhala moyo waumulungu, wolemekeza Khristu. Mu ntchito ya Mulungu, palibe chofunika kwambiri. Komabe, n'zomvetsa chisoni kuti mipingo ndi mabungwe ambiri a Chipentekoste akukanthidwa ndi amuna ndi akazi achinyengo amene chifukwa cha umunthu wawo wamphamvu, apeza malo otchukirapo m'gululi. Amenewa ali mu "zovala zankhosa koma m'kati mwao ali mimbulu yolusa" nabweretsa manyazi ku mpingo (Mateyu 7:15).

Baibulo limanena za anthu osaopa Mulungu oterowo. Mwachitsanzo, Paulo anachenjeza akulu a ku Aefeso za "mimbulu yosautsa" imene idzalowe ndi kuwononga gulu la nkhosa za Mulungu (Machitidwe 20:29). Mu uthenga womwewo, anawakumbutsa mmene anawatsogolera ndi mtima wosagawanika. "Sindinasilira siliva, kapena golidi, kapena chobvala cha munthu aliyense,"

anatero Paulo (Machitidwe 20:33). Mofananamo, iye anakumbutsa Atesalonika za khalidwe lake laumulungu pakati pawo, kuti, "Inu ndinu mboni, Mulungunso, kuti tinakhala oyera mtima ndi olungama ndi osalakwa kwa inu akukhulupirira" (1 Atesalonika 2:10). Paulo sanangotsogolera ndi ulamuliro ndi kutumikira ndi mphamvu, anali kukhala ndi umphumphu waumulungu. Ifenso tiyenera kuchita chimodzimodzi masiku ano.

Kumvetsetsa

Chachiwiri, ngati Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kumvetsetsa bwino udindo wanu wopatsidwa ndi Mulungu. Muyenera kutumikira Khristu ndi mpingo wake mokhulupirika potsogolera anthu a Mulungu kupititsa patsogolo utumwi mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Mungapeze kumvetsetsa kumeneku kuchokera m'magwero awiri: kuchokera m'Mawu a Mulungu ndi mwa Mzimu wa Mulungu. Mwakuphunzira Malemba mokhulupirika, mudzazindikira ntchito ya Mulungu yowombola mitundu ya anthu. Mwa kupemphera ndi kutchera khutu ku mawu a Mulungu, mudzazindikira udindo wanu wapadera pokwaniritsa ntchito imeneyi.

Yesu amamvetsetsa bwino lomwe malo ake mu dongosolo la chiowombolo cha Mulungu. Nthawi zambiri ankalankhula za ntchito yake (Marko 10:45; Yohane 6:38; 18:37). Iye ananena, "Pakuti Mwana wa Munthu anadza kudzafunafuna ndi kupulumutsa chotaikacho" (Luka 19:10). Mofananamo, Paulo anamvetsetsa udindo wake wapadera m'ntchito ya Mulungu. Iye analemba, "Umene anandiika ine mlaliki wake ndi mtumwi (ndinena zoona, wosanama ine), mphunzitsi wa amitundu m'chikhulupiriro ndi choonadi" (1 Timoteo 2:7).

Kupyolera m'pemphero latsiku ndi tsiku ndi kusanthula Baibulo, inu, monga Yesu ndi Paulo, mukhoza kumvetsa bwino utumwi wa Mulungu, ndi udindo wanu waumwini pokwaniritsa utumwiwo.[1]

Kudzipereka

Chachitatu, monga mtsogoleri wa Chipentekoste, musangozindikira chabe utumwi wa Mulungu, mudzipereke kwathunthu kuchita mbali yanu kukwaniritsa utumwiwo. Utumwi wa Mulungu, nthawi zina umatchulidwa *missio Dei,* ndi

[1] Kuti mudziwe zambiri za utumwi wa Mulungu, onani buku la Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Chiphunzitso cha M'baibulo cha Utumwi*, lolembedwa ndi Paul York.

cholinga ndi ntchito yake mu dziko lapansi molingana ndi mtundu wa anthu wakugwa. Iye amagwira ntchito kudzera mu Mpingo wake kuti adziyitanire yekha anthu kuchokera m'fuko lililonse, chilankhulo chilichonse, mitundu iliyonse pa dziko lapansi (Chivumbulutso 5:9; 7:9).

Pamene maganizo a anthu ena atha kuchoka mu utumwi wa Mulungu, chidwi chanu chikhalebe cholunjika pakuchita chifuno cha Mulungu. Zolingalirandi zochita zanu ziyende munjira ya utumwi wa Mulungu. Monga mtsogoleri wa Chipentekoste, mugwire cholinga chonse cha Mulungu – dongosolo la Mulungu lowombola mafuko. Mudzindikirenso pamene mpingo wanu ukupeza malo mudongosolo limenelo. Mukatero, muyendetse mpingo munjira imeneyo.[2]

Kudzoza

Chachinayi, monga mtsogoleri wa Chipentekoste, muchitire ulemu kudzodza kwa Mzimu, komanso muyesetse kusunga kukhudza kwa Mzimu pamoyo wanu mwa kudzipereka m'pemphero, kukhala mwachiyero, ndi utumiki wodzichepetsa. Muyenera kudalira mwa mphamvu pa Mzimu Woyera kuti akudzodzeni, akuthangatireni, komanso kukutsogolerani mu utumiki. Ndipo mutengere kumtima mawu akuchoka kwa Ambuye onenedwa kwa ophunzira ake, pamene anawalamulira iwo kuti asayambe kutumikira kufikira atavekedwa mphamvu mwa Mzimu Woyera (Machitidwe 1:4-5; Luka 24:49).

Kudzichepetsa

Chachisanu, monga mtsogoleri woona wa Chipentekoste, muziwone nokha ngati kapolo wa Mulungu komanso anthu ake. Mufunefune kutsata chitsanzo cha Mbuye wanu, amene anadzichepetsa yekha nakhala kapolo, kufikira imfa yapamtanda (Afilipi 2:7-8). Ndipo mukhale wokumbukirabe mawu a Yesu: "koma amene aliyense afuna kukhala wamkulu mwa inu adzakhala mtumiki wanu ; ndipo amene aliyense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la kwa anthu ambiri" (Marko 10:43-45).

Mtundu wa utsogoleri uwu umatchedwa utsogoleri wotumikira. Mosiyana ndi izi, mtsogoleri amene adzikuza yekha nafunafuna kukhutitsa zofuna zake pa anthu

[2] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kutsogolera mpingo ku utumwi wa Mulungu, onani Mutu 31: "Utsogoleri wa Utumwi."

a Mulungu sangatchulidwe mtsogoleri woona wa Chipentekoste. M'malo mwake ndi "mimbulu m'chovala cha nkhosa" (Mateyu. 7:15-16; Machitidwe 20:29-30). Baibulo limatiwuza ife, "usakhale ndi chochita ndi anthu oterowo" (2 Timoteo 3:5).[3]

Luso

Chomaliza, monga mtsogoleri woona wa Chipentekoste, muyesetse kukhala wa luso. Mwayenera kuzindikira kuti, kukhala munthu wabwino kuli mbali imodzi yofunikira, koma sizokwanira. Mafirika amadziwidwa monga anthu abwino, odzichepetsa, komanso ocheleza bwino alendo. Kukhala mtsogoleri wabwino, komabe, kudzafuna iwe utukule maluso ena ake. Maluso amenewa akuphatikiza kutha kuphunzitsa, kuponya masomphenya, kutakasa ena, komanso kulongosola ntchito.

Kuwonjezera apo, mumvetsetse kuti, m'chimake chenicheni, kuthekera kwa utsogoleri kumachokera kwa Mulungu. Paulo ankachidziwa ichi mwakuya. Anafotokoza kwa Akorinto, "sikuti tiri okwanira pa ife tokha, kuyesera kanthu monga mochokera mwa ife tokha; kukwanira kwathu kuchokera kwa Mulungu; amenenso anatikwaniritsa ife tikhale atumiki…a mzimu" (2 Akorinto 3:5-6). Monga mtsogoleri wa Chipentekoste, muyang'ane mokhazikika pa Mulungu kuti mulandire luso lotere.

ZOCHITA ZA MTSOGOLERI WA CHIPENTEKOSTE

Mbusa wa Chipentekoste asakhale ngati Mbusa wina amene anawonedwa akuthamanga kuseri kwa mpingo wake akufuula, "Ndidikireni ine, ndine mtsogoleri wanu!" Mosiyana ndi izi, iye apite patsogolo pa anthu, kuwadandaulira iwo atsatire. Akhale ngati Yesu, amene adakodola ophunzira ake, "Bwerani munditsate, ndipo ndikutumizani mukasodze anthu." Baibulo limatiuza ife, "Nthawi yomweyo iwo anasiya makoka awo ndi kumutsatira" (Marko 1:17-18).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, Khristu wayikidza inu muyambitse mu mpingo zilongosoko ndi ndondomeko zouzilidwa ndi Mzimu. Pamenepo mutakase anthu a Mulungu atsate inu mu ntchitoyi. Pa nthawi yomweyo, monga mtsogoleri wa umulungu, mukhale wotsatira wodzipereka. Mutsatire Mzimu wa

[3] Kuti muunikiridwe kwambiri pa utsogoleri wotumikira, onani Mutu 29: "Utsogoleri Wotumukira."

Mulungu mokhulupirika. Ndipo modzichepetsa mudzipereke kwa iwo amene Mzimu wayika pamwamba panu. Mutsogolere mpingo wanu kukwaniritsa utumwi wa Mulungu njira zitatu zofunikira:

Kuponya Masomphenya

Choyamba, mutsogolere anthu anu mwa kuponya masomphenya atsogolo losankhika la mpingo. Mwa mawu ena, muwathandize iwo kuwona tsogolo lodabwitsa limene Mulungu waakonzera iwo. Pamenepo, uwakoke iwo kuyenda mu njira imeneyo. Umachita ichi ndi mawu ako, ndi zochita zako, ndi malingalilidwe ako, kutanthauza ndi zimene umalankhula, zimene umachita, komanso m'mene umaziperekera wekha ku anthu.

Masomphenya ako wouzilidwa ndi Mulungu akuyenera anyeketse iwe kufikira kuti sungazitaye. Zikatere, udzakhala mopitiliza ukulankhula za masomphenya ako. Chikhumbo chako chidzayenda kutuluka m'moyo wako ndikukhuza anthu, kuwachititsa iwo kugawana nawo masomphenya. Monga mtsogoleri weniweni wa Chipentekoste, osayelekeza kukweza masomphenya a mtsogolo a iwe mwini. Koma iwe ukweze masomphenya a Mulungu monga avumbulutsidwa m'Mawu ake mwa Mzimu Woyera.

Baibulo limatiuza ife, "Pamene palibe vumbulutso, anthu amataya kudziletsa" (Miyambo 29:18). Kapena, monga matanthauzilidwe ena anena, "Pamene palibe masomphenya auneneri anthu amakhumudwa." Kukhumudwa kotere nthawi zambiri kumathera kudzitukumula wekha, kugwa, ndipo mapeto ake chiwonongeko. Komabe, masomphenya wolankhulidwa bwino adzachititsa anthu kuzindikira:

1. *Chimene anthuwo ali*. Iwo ali anthu autumwi olimbitsidwa ndi Mzimu wa Mulungu, olembedwa ntchito ndi Khristu kukadandaulira m'dziko lapansi.

2. *Kumene anthuwo apite.* Akuyenela ayende pamodzi kukwaniritsa utumwi wa Mulungu m'kukopa otayika, kudzala mipingo yatsopano, komanso kutengapo mbali m'kutumiza atumwi ku mafuko.

3. *Chimene anthuwo achite.* Iwo akhale olimbikitsidwa ndi Mzimu komanso odzipereka kukuchita mbali yawo mu kukwaniritsa utumwi wake.

4. *M'mene anthuwo achitire.* Mbusa afotokoze momveka dongosolo lapadela kapena ndondomeko ya m'mene ntchitoyo ingakwaniritsidwire. Iye awawonetsere pamenepo anthuwo m'mene iwo angatengele mbali mu ntchitoyo.

5. *M'mene ayambire.* Mbusa wochitachita wa Chipentekoste adzapereka zochita kwa anthu kuwathandiza ayambe bwino.

Mwachisoni, maloto ambiri opatsidwa ndi Mulungu amafela mu mtima mwa Mbusa. Koma, iwe usalore izi zichitike. Mokhulupilika uponye masomphenya a tsogolo lokoma la mpingo. Iwe uyime chilili komanso molimba mtima kuwuza anthuwo, "Njira ndi iyi; yendani mmenemo" (Yesaya 30:21).[4]

Kuyang'anira

Chachiwiri, pakati pakudzindikira kumene Mulungu akufuna mpingo wanu ukhale ndi kufikira chimenecho, pali njira yoti mudutsemo. Monga oyimirira Mulungu, mutsogolere mpingo munjira imeneyo. Inu musangoponya chabe masomphenya a tsogolo lokoma la Mulungu, muyang'anirenso chikwaniritso cha masomphenyawo.

Ichi ndichimene Yesu anachita. Iye anaponya masomphenya, ndipo kenako anagwiritsa ntchito ndondomeko kukwaniritsa masomphenyawo. Ndondomeko yake inali kuyitana amuna ndi akazi kumbali yake, kuwaphunzitsa, kuwapatsa ntchito, kuwapatsa mphamvu, ndikukawatuma ku ntchitoyo. Monga mtsogoleri wa Chipentekoste, muchitenso chimodzimodzi. Mungathe kuchita ichi kupyolera m'dongosolo, kugwedeza anthu ayambe kuyenda, komanso kuyang'anira, zonse mwa kuuzira kwa Mzimu.

Choncho, monga Mbusa wa Chipentekoste, sulipo chabe kungotakasa anthu ako, ukuyenera uyang'anire ntchito (1 Tim. 3:1-2; Tito 1:7). Monga wong'anira, ulipo kugwirizanitsa mpingo ku utumwi wolimbitsidwa ndi Mzimu. Ukwanitse kuyang'anira ukatakwe ndi zochita zoyenela kuti dongosolo likwaniritsidwe. Zochita zimenezi zikuphatikiza kupeza oti agwire ntchito, kupanga dongosolo, kuwaphunzitsa, komanso kuwatumiza ku malo a ntchito. Mu ichi chonse, uyang'ane kwa Mzimu Woyera kufuna mnzeru ndi chitsogozo.

---

[4] Kuti mudziwe zambiri za kuponya masompheya, onani Mutu 30: "Utsogoleri Wamasomphenya."

Kupititsa Chitsogolo

Chomaliza, monga mtsogoleri wa anthu a Mulungu, mumanyamula udindo wotanamphitsa ndi kupititsa chitsogolo masomphenya autumwi wa Mulungu. Njira imodzi yochitira ichi ndipakudzutsa ena atsogoleri a Chipentekoste wokhala ndi masomphenya. Ngati ichi sichinachitidwe, masomphenyawo adzafa, ndipo utumwiwo udzakanika. Ndizomvetsa chisoni kuti mautumiki ambiri oyikidwa ndi Mulungu afa pamodzi ndi oyambitsa awo chifukwa amuna ndi akazi amenewa analephela kuikiza mwa ena masomphenyawo mokwanira.

Koma, Yesu anali woyikapo mtima pakuwolotsera masomphenya ake kwa ena. Mosachedwa atangoyamba utumiki wake, anayamba kuyitana ophunzira ake. Baibulo limati, "Anasankha khumi ndi awiri kuti akakhale naye ndi kuti awatume kukalalikira" (Marko 3:14; 1:16-17; 2:13-14; 3:13-19). Amuna amenewa anali oti adzanyamula ntchitoyo Iye atapita. Iye motero anawaphunzitsa, nawapatsa mphamvu, komanso kuwatumiza "mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse" (Mateyu 28:19). Mwa mawu ena, Yesu anayembekezera iwo kukachita ndi ena monga Iyenso anachita nawo iwowa.

Paulo anatsanza chitsanzo cha Yesu. Iye sanachite utumiki wake wa utumwi yekha, koma anayitana ena kuzilumikiza kwa iye. Kenako anawawumba nawaphunzitsa, monganso Yesu anachita ndi ophunzira ake. Ophunzira a Paulo anaphatikiza Yohane Marko, Timoteo, Tito, Luka ndi ena. Paulo anamulangiza Timoteo kuchita ndi ena monga iye anachitanaye. "Zinthu zomwe mwandimva ndikunena," iye analembera mwana wake m'chikhulupiriro, "ikiza kwa anthu odalirika amenenso adzakhala oyenerera kuphunzitsa ena" (2 Tim. 2:2).Ngati ife tifuna kupititsa chitsogolomasomphenyawo mwa ena, ife titsanze m'mapazi a Yesu ndi Paulo.

Paulo anadandaulira okhulupirira m'Tesalonika, "Pakuti mudziwa nokha m'mene muyenera kutitsanza ifemo," chifukwa, iye anati, "pakuti sitinakhala dwakedwake mwa inu" (2 Ate. 3:7, 9). Ngati ife tifunadi kupititsa patsogolo lero masomphenya autumwi wa Chipentekoste, ngati Paulo, tikhale mtundu wa munthu umene ena adzakonde kutsanza. Kutanthauza, ife tikhale anthu olemekezeka, aungwiro, komanso a masomphenya.

Monga mtsogoleri woyikidwa ndi Mulungu, ukakhale mtsogoleri woposera yemwe ungathe kukhala. Monga mtsogoleri wokhulupilika wa Chipentekoste, ulimbike kutukula maluso a utsogoleri oyenela kukwaniritsira udindowu.

~ Mutu 29 ~

Utsogoleri Wotumikira

Tsiku lina gulu lina la ophunzira a Yesu linamuyandikira ndi funso. Iwo anafunsa, “Ndani kodi ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba?” (Mat. 18:1). Ophunzira awa anakhala akutsutsana fundo imeneyi pakati pawo (Mat. 20:20-28; Marko 9:33-37; 10:35-45; Luka 22:24-27). Ena mwa iwo anali ozikankhira ndipo amafuna kusanduka atsogoleri pa ophunzirawo.

Podziwa mitima yawo, Yesu anaitana kamwana kabwere ndikuyimilira pakati pa iwo. Kenako Iye anati kwa ophunzira ake, “Indetu ndinena kwa inu, Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato, simudzalowa konse mu Ufumu wa Kumwamba. Chifukwa chake yense amene adzichepetsa yekha monga kamwana aka, yemweyo ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba” (Mat. 18:3-4). Pa nthawi yina, Yesu anafotokozera, “Mudziwa kuti mafumu a anthu amadziyesa okha ambuye awo, ndipo akulu awo amachita ufumu pa iwo. Sikudzakhala chomwecho kwa inu ai; koma aliyense amene akafuna kukhala wamkulu mwa inu, adzakhala mtumiki wanu; ndipo aliyense amene akafuna kukhala woyamba mwa inu, adzakhala kapolo wanu” (Mat. 20:25-27).

Yesu amalankhula za mtundu wa utsogoleri omwe Iye akufuna ukhale mu Mpingo wake umene ukuwumbidwa mwatsopano. Atsogoleri mu Mpingo wake adzayembekezeledwa kutsogolera mosiyana kwambiri ndi atsogoleri a m’dziko. M’malo motumikiridwa, atsogoleri atsopano amenewa adzatumikira ena. M’malo molamulira anthuwo, iwo adzasamalira mwachikondi iwo amene akuwatsogolera.

Mtundu wa utsogoleri uwu tsopano umatchedwa utsogoleri wotumikira. Umenewu ndi mtundu wa utsogoleri omwe Mulungu akulamulira pa atsogoleri a Chipentekoste m'Afirika lero.

KUTAMBASULA UTSOGOLERI WOTUMIKIRA

Utsogoleri ndi kuthekera kokopa anthu achite njira inayake kapena kusuntha m'mbali inayake. Kwa Mbusa wa Chipentekoste, utsogoleri ndi kuthekera kopatsidwa ndi Mulungu kukakopa anthu a Mulungu kuti ayambe athanga ufumu wa Mulungu (Mat. 6:33). Uku ndi kuthekera kotakasa anthu a Mulungu kukakwaniritsa ntchito yawo yopatsidwa ndi Mulungu m'kupambanitsa utumwi wa Mulungu m'dziko lapansi.

Monganso atsogoleri onse, atsogoleri otumikira ali okhudzika ndi utumwi. Komabe, atsogoleri otumikira ali okhudzikanso ndi kukula komanso ukoma wa anthu omwe iwo akuwatsogolera. Iwo amatumikira anthu a Mulungu ndi kudzichepetsa komanso chifundo, ndipo amayetsetsa kukopa kupyolera mchikondi osati kuwalamulira.

Maganizidwe a mtsogoleri wotumikira ali motsutsana ndi "maganizidwe aunyakwawa" amene timawawona nthawi zambiri mu Afirika. Nyakwawa yopanda Mulungu imalamulira mwa kuwopsezana; pamene mtsogoleri wotumikira amatsogolera mwa chikondi komanso chifundo. Nyakwawa imakakamiza kumveledwa; pamene mtsogoleri wotumikira amatakasa chitsimikizo mtima. Nyakwawa imapezerapo zokomela iyo pa anthu; mtsogoleri wotumikira amasakasaka awadalitse iwo.

Yesu akanatha kulamulira ngati ichitira nyakwawa; koma, Iye anasankha kutsogolera ngati wotumikira (Mat. 20:28). Pa nthawi iliyonse, akanatha Yesu kulamula makamu a angelo achite chifuno chake (Mateyu 26:53). Komabe, Iye anasankha kudzichepetsa yekha ndi kudzipereka yekha ku chifuno cha Atate wake (Mat. 26:39, 42). Nsembe yake ya pa mtanda ili chitsanzo chenicheni cha tanthauzo la kukhala mtsogoleri wotumikira. Monga Mbuye wawo, abusa enieni a Chipentekoste amakhala atsogoleri otumikira. M'malo mokwaniritsa zokomela iwo pa otsatira awo, iwo amawatumikira mokondwera ndi mwachikondi.

Ufumu wa Mulungu waonetsedwa ngati "ufumu wachadodolido" (kusanduliza zinthu). Ichi chili chifukwa utsogoleri mu ufumu wa Mulungu umachita mosiyana ndi utsogoleri wa ndondomeko ya m'dziko lapansi. M'mabungwe a dziko lapansi, mtsogoleri ndi amene amayembekezeredwa akhale

iye wapamwamba. Iye amalamulira ena komanso kulandira ulemelero wochuluka pamodzi ndi phindu lochuluka. Koma, mu ufumu wa Mulungu, mtsogoleriyo ndi amene amakhala pansi. Iye amayetsetsa kutumikira komanso kudalitsa ena.

MAKHALIDWE A MTSOGOLERI WOTUMIKIRA

Makhalidwe asanu ndi amodzi akuyenela apedzeke mwa Mbusa aliyense wa Chipentekoste amene afunafuna kukhala mtsogoleri wotumikira:

Kudzichepetsa

Choyamba, monga mtsogoleri wotumikira, Mbusa wa Chipentekoste akuyenela atsogolere ndi kudzichepetsa. Iye asataye nthawi ndi kusakasaka kulemekezedwa kapena mphamvu. M'malo mwake, iye atsanze chitsanzo cha Yohane M'batizi, amene anatero za Yesu, "Iye akule; ine ndichepe" (Yohane 3:30). Ndipo iwo akumbuke mawu a Mbuye wawo: "Koma wamkulu wopambana wa inu adzakhala mtumiki wanu. Ndipo amene ali yense akadzikuza yekha adzachepetsedwa; koma amene adzichepetsa mwini yekha adzakulitsidwa" (Mat. 23:11-12).

Pali mkhalidwe wotsautsa pakati pa abusa a m'Afirika kudzitchulira okha mayina apamwamba. Yesu anachenjeza motsutsana ndi mchitidwe umenewu. Iye anawauza ophunzira ake, "Koma inu musatchedwa, Rabi; pakuti Mphunzitsi wanu ali mmodzi, ndipo inu nonse muli abale. Ndipo inu musatchule wina atate wanu pansi pano, pakuti alipo mmodzi ndiye Atate wanu wa Kumwamba. Ndipo musatchedwa atsogoleri, pakuti alipo mmodzi Mtsogoleri wanu, ndiye Khristu. Koma wamkulu wopambana wa inu adzakhala mtumiki wanu" (Mat. 23:8-11). Amuna ndi akazi oganiza mochepa nthawi zambiri amafunafuna mayina akulu. Koma, atsogoleri aakuludi amakhala okhutila kuwonedwa monga akapolo a Khristu.

Usiku wotsogolera kupachikidwa kwa Yesu, Iye anakumana ndi ophunzira ake m'chipinda cha pamwamba mu Yerusalemu. M'menemo anawaphunzitsa iwo phunziro pa utsogoleri wotumikira. Atatha chakudya cha Paska, Mpulumutsiyo anayimilira, nachotsa chobvala chake chapamwamba, natenga nsalu youmitsira madzi nayimanga m'chiuno mwake. Kenako Iye anatenga beseni muli madzi nayamba kusambitsa mapazi a ophunzira ake. Atamaliza,anawafunsa, "Nanga chimene ndakuchitirani inu, muchizindikira kodi?"

Kenako Yesu anafotokozera iwo, “Inu munditcha Ine Mphunzitsi, ndi Ambuye: ndipo munena bwino; pakuti ndine amene. Chifukwa chake, ngati Ine Ambuye, ndi Mphunzitsi, ndasambitsa mapazi anu, inunso muyenera kusambitsana mapazi wina ndi mnzake. Pakuti ndakupatsani inu chitsanzo, kuti, monga Inendakuchitirani inu, inunso muchite” (Yohane 13:13-15). Yesu amaphunzitsa ophunzira ake kuti atsogoleri aakulu mu ufumu wake ndi iwo amene adzichepetsa okha mpaka ku udindo wapansi wotumikira mnyumba.

Monga Mbusa wa Chipentekoste, choncho, ukane molimba zikoka zovunda za mphamvu pawanthu komanso kunyada. Monga mtsogoleri wotumikira weniweni, usayelekeze konse kukwaniritsa zokomela iwe pa anthu a Mulungu. M’malo mwake, ufunefune kutumikira ndi kudalitsa ena.

Chifundo

Chachiwiri, monga mtsogoleri wotumikira weniweni, Mbusa wa Chipentekoste akuyenela amve chifundo ndi anthu amene wayitanidwira kuwatsogolera. Kumva chifundo ndi wina ndikudziyika m’gulu limodzi ndi iye komanso kugawana mamvedwe, zowawa mtima, ndi chisangalalo. Baibulo limalankhula kuti Yesu ndi Wankulu Wansembe wathu wankulukulu wokhonza “kumva chifundo ndi zofooka zathu” (Ahebri 4:15). Iye anamvera chifundo Maria ndi Marita pamene Iye analira pamodzi ndi iwo kumanda a Lazaro (Yohane 11:35). Monganso Yesu, iwe ngati mtsogoleri wotumikira, uphunzire ku “Kondwani nawo iwo akukondwera; lirani nawo akulira” (Aroma 12:15).

Chilungamo

Chachitatu, monga mtsogoleri wotumikira, Mbusa wa Chipentekoste ayesetse kukhala owonekera mu zochita zake zonse ndi anthu. Ichi chikutanthauza kuti iye sayesera kubisira ena chenicheni chimene ali. Iye savala chigoba kuti awoneke chinthu chimene sanakhale. Paulo anawakumbutsa Akorinto za kusazibisa. Iye analemba, “Pakuti kudzitamandira kwathu ndiko umboni wa chikumbumtima chathu, kuti m’chiyero ndi kuona mtima kwa Mulungu, si m’nzeru ya thupi, koma m’chisomo cha Mulungu tinadzisunga m’dziko lapansi, koma koposa kwa inu” (2 Ako. 1:12). Iye anawonjezera mtsogolo mwake, “M’kamwa mwathu mmotseguka kwa inu aKorinto, mtima wathu wakulitsidwa” (2 Ako. 6:11).

Kusazibitsa kotero kudzatsekula madanga akulankhulana pakati pa iwe ndi ma membala a mpingo wako. Anthu adzayamba kukuwona iwe monga munthu

woona mtima, munthu wodalilika. Mapeto ake, iwo adzakhala olimbikitsika kukudalira komanso ku ulula zowasautsa. Ndipo adzakhala okondwa kutsatira utsogoleri wako.

Chidaliro

Chachinayi, monga mtsogoleri wotumikira, Mbusa wa Chipentekoste adzadalira anthu a Mulungu. Iye adzakhulupirira kuti Mzimu Woyera yemweyo amene akhala mkati mwake, nampatsa mphamvu komanso kumtsogolera iye, akukhalanso mkati mwa mamembala ake, kuwapatsa mphamvu ndikuwatsogolera. Chifukwa cha ichi, Mbusa wa Chipentekoste amatha kudalira anthu a Mulungu, ndipo iye amakhala wofunadi kupatsa mphamvu za utumiki kwa ena. Ichi ndi chimene Yesu anachita kwa ophunzira ake khumi ndi awiriwo (Yohane 20:21). Ndipo ichi ndichimene Paulo anachita ndi Timoteo (2 Timoteo 2:2). M'malo moyesera yekha kuchita ntchito khumi, Mbusa wochitachita adzapatsa mphamvu kwa mamembala khumi achite ntchito zimenezo.

Choncho, monga mtsogoleri wotumikira wokhulupilika, muzindikira mphatso za Mulungu mwa ena. Ndipo mukhale ndi nthawi ndi iwo, kuwathekeretsa ndi kuwaphunzitsa iwo kuchita ntchito yabwino. Pamene atsogoleri odzukawa akukula m'kudzindikira kwawo ndi kuthekera, mudzafuna kuwatuma mu udindo wochulukirapo. Pakuwatuma, muwapatsenso iwo ulamuliro umene asowekere kuti akwaniritse mogwira ntchito zawo zatsopano.

Mtsogoleri wamkulu sawopsedwa ndi chipambano cha ena. M'malomwake, chimwemwe chake chachikulu chibwera m'kudzutsa ena amene atenge mbali m'kukwaniritsa utumwi.

Kulankhulana

Chachisanu, monga mtsogoleri wotumikira, Mbusa wa Chipentekoste aphunzire kulankhula bwino ndi iwo akuwatsogolera. Kulankhulana bwino kumaphatikiza kulankhula mwamzeru ndi kumvetsera momvetsetsa. Baibulo limadandaulira, "Mau anu akhale m'chisomo, okoleretsa, kuti mukadziwe inu mayankhidwe anu a kwa yense akatani" (Akolose 4:6). Ilo limatilangizanso ife kukhala"wofulumira [kapena wokonzeka] kumvetsera" (Yakobo 1:19). Choncho, monga mtsogoleri wotumikira wochitachita, uike nthawi yambiri komanso mphamvu mukusanduka wolankhula mochititsa chipambano.

Kudzoza

Chomaliza, monga mtsogoleri wotumikira, Mbusa wa Chipentekoste afunefune kudzoza kwa Mzimu Woyera. Iye awonetsetse kuti atsogoleri enanso mu mpingowo akuchita zomwezo. Kudzoza kumalandiridwa pamene munthu wabatizidwa mwa Mzimu Woyera monga zinachitika ndi ophunzira pa Tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2:4). Iko kumasungika mwa kuyenda mu Mzimu Woyera (Agalatiya 5:25).

Yesu ndi chitsanzo chapamwamba cha m'mene umawonekera utsogoleri wotumikira wodzodzedwa ndi Mzimu. M'mene Yesu ankayamba utumuki wake, Iye analengeza kuti Mzimu Woyera anamudzodza kukatumikira ena m'zosowa zawo (Luka 4:18-19). Petro anafotokozera za utumiki wotumikira wa Yesu motere: "Mulungu anamdzoza Iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nachita zabwino, nachiritsa onse osautsidwa ndimdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi Iye" (Mach. 10:38).

Monganso Yesu, ife tisayesere kuchita ntchito ya Mulungu mu mphamvu zathu kapena kuthekela kwathu. M'malomwake, tidalire pa mphamvu ndi kudzodza kwa Mzimu (Luka 24:49; Machitidwe 1:8).

ZITSANZO ZA UTSOGOLERI WOTUMIKIRA

Baibulo lili ndi zitsanzo zambiri za utsogoleri wotumikira. Tiyeni tiwone zitsanzo zinayi. Ziwiri zikupezeka m'Chipangano Chakale, ndipo ziwiri zina zikupezeka m'Chipangano Chatsopano.

Mose: Utumiki Wopatsidwa

Mose ndi chitsanzo chabwino cha mtsogoleri wotumikira amene anali wodzichepetsa ndithu mpaka kupatsa utumiki kwa ena. Mulungu anayika pa Mose ulamuliro waukulu pakumusankha iye atsogolere anthu ake (Eksodo 3:1-10). Nthawi zambiri Mulungu analankhula ndi Mose "maso ndi maso monga munthu amalankhula ndi bwenzi" (Eksodo 33:11). Ndipo Mulungu anagwiritsa nntchito Mose kuchita zizindikilo ndi zodabwisa zazikulu pakati pa anthu (Eksodo 4:21; Machitidwe 7:36). Komabe, Mose sanasanduke wonyada. M'malomwake, iye anasankha kutsogolera anthu a Mulungu ndi kudzichepetsa (Numeri 12:3).

Baibulo limatiuza nkhani ya m'mene apongozi amuna a Mose anamulangizilira iye achitire ntchito yake (Eksodo 18:13-27). Pamene Yetero

anamuwona Mose akuchita ntchito yonse yekha, anamulangiza mkamwini wake "Chinthu uchita'chi sichiri chabwino ai… pakuti chikulaka chinthu ichi; sungathe kuchichita pa wekha." (Eksodo 18: 17-18). Mose anatsatira langizo la Yetero napatsa ntchito yambiri kwa amuna odalilika. Chotsatira chake, Mose anapepukidwa, ntchitoyo inapambana, komanso anthu anadalitsika.

Davide: Anakweza Ena

Chitsanzo china chabwino cha mtsogoleri wotumikira ndiDavide. Mulungu anakamba za iye ngati "munthu wa pamtima wanga" (Machitidwe 13:22; 1 Samuele 13:14). Chifukwa choti Davide analiwotetezeka mu udindo wake ngati mfumu komanso ngati mtumiki wa anthu a Mulungu, iye anakwanitsa kuyikiza nthawi ndi mphamvu m'kuwumba ena.

Pokhala mtsogoleri wotumikira wodzichepetsa, Davide sanachita mantha ndi chipambano cha anthu ena monga anachita wapambuyo pake, Sauli. Davide anazizinga yekha molimbamtima ndi iwo amene zipambano zawo zinanga zake zomwe (1 Mbiri 11:10-47). Ndipo analemekeza iwo amene anatumikira pansi pake, kuwalimbikitsa akapambane (1 Mbiri 11: 17-19, 25). Mulungu anagwiritsa nntchito mtima wofuna wa Davide kukweza ena alimbitse chipambano chake komanso kudalitsa onse amene anatumikira pansi pa iye.

Paulo: Mphunzitsi Waumulungu

Chitsanzo chachitatu cha mtsogoleri wotumikira wodzichepetsa ndi mtumwi Paulo. Ngakhale Mulungu anamuyitana akhale mtumwi, anaziwona yekha ngati kapolo wa Khristu (Aroma 1:1; Tito 1:1). Paulo anakambaponso za yekha ngati "wang'ono wa atumwi" (1 Akorinto 15:9). Iyenso anaphunzitsidwa ndi Barnabasi (Machitidwe 9:26-27; 11:25-26). Panthawi yake, anaphunzitsa ena mwakhama. Makalata ake amavumbulutsa m'mene iye anafunira mosalekeza kuwumba ena.

Ziwiri mwa zipambano zazikulu kwambiri za Paulo ndi Timoteo komanso Tito. Anaphunzitsa Timoteo (Machitidwe 16:1-5), ndipo m'kudutsa kwa nthawi anadalira "mwana wake mchikhulupiriro" kukatsogolera mpingo mu Aefeso (1 Timoteo 1:2-3). Iye anaphunzitsanso Tito kenako namuyika atsogolerere mipingo m'Krete (Tito 1:5). Akanakhala kuti mtumwiyo sanatenge mphamvu ndikuphunzitsa Timoteo, Tito, ndi ena, chikoka chake ndi ntchito yake zikanazilala kwakukulu.

Yesu Khristu: Chitsanzo Chapamwamba

Ambuye Yesu Khristu ayima ngati chitsanzo chapamwamba cha utsogoleri wotumikira. Iye anaphunzitsa kuti atsogoleri eni-eni a ufumu amatumikira ena mosadzikonda (Luka 22:24-27). Kenako, Iye anawonetsera nfundoyi m'moyo wa Iye yekha komanso mu utumiki wake. Polankhula za Iye yekha, Yesu anati, "Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la kwa anthu ambiri" (Marko 10:45). Pauloanafotokoza za machitidwe a utsogoleri wotumikira wa Yesu motere:

"Mukhale nawo mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu, ameneyo pokhala nawo maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu ; ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pa mtanda!" (Afilipi 2:5-8).

Paulo anadandaulira Akhristu onse motere, kuwonjezelapo atsogoleri a Chikhristu, "musachite kanthu monga mwa chotetana, kapena monga mwa ulemerero wopanda pache, komatu ndi kudzichepetsa mtima, yense ayese anzake omposa iye mwini; munthu yense asapenyerere zake za iye yekha, koma yense apenyererenso za mnzake" (Afilipi 2:3-4).

MADERA A UTSOGOLERI WOTUMIKIRA

Maganizidwe a utsogoleri wotumikira adziwonetsere wokha m'madera atatu a moyo wa Mbusa wa Chipentekoste komanso utumiki wake: kunyumba, ku mpingo, ndi dera lanu.

Utsogoleri Wotumikira M'nyumba

Monga Mbusa wa Chipentekoste, dera lanu loyamba la utsogoleri wotumikira ndi m'nyumba mwako. Usanatumikire mpingo wako, utumikire wapabanja wako ndi ana ako mokhulupilika. Paulo anati za oyang'anira, kapena Mbusa, "woweruza bwino nyumba yake ya iye yekha, wakukhala nawo ana ake omvera iye ndi kulemekezeka konse" (1 Timoteo 3:4). Paulo anawonjezeranso, "Koma ngati munthu sadziwa kuweruza nyumba ya iye yekha, adzasunga bwanji mpingo wa Mulungu ?" (v. 5).

Choncho, monga Mbusa wa Chipentekoste, ukhale wodziwa nthawi zonse kuti dera lako loyamba la utsogoleri wotumikira lili m'banja lako. Ukhale ndi mtima wofuna kudzichepetsa wekha ndi kutumikira wapabanja wako komanso ana ako. M'lingaliro lina, banja lako ndi "mpingo wako Woyamba," ndipo mpingo umene ukutsogolera uja ndi "mpingo wako wowonjezera." Maganizidwe amene utumikira nawo banja lako mosalephera adzakhalansomaganizidwe amene udzatumikira nawo mpingo wako. Iwe ukhale mtsogoleri wotumikira kuziwiri zonse.

Utsogoleri Wotumikira Mumpingo

Dera lanu lachiwiri la utsogoleri wotumikira ndi mpingo. mudziwone nokha monga mphatso ya Khristu ku mpingo (Aefeso 4:11-12). Kuwonjezera apo, mudzindikire kuti Yesu wakuyitana iwe ubuse anthu a Mulungu. Petro analembela akulu: "Wetani gulu la Mulungu lili mwa inu, ndi kuliyang'anira, osati mokakamiza, koma mwaufulu, kwa Mulungu ; osatsata phindu lonyansa, koma mwa changu ; osati monga ochita ufumu pa iwo a udindo wanu, koma okhala zitsanzo za gululo" (1 Pet. 5:2-3).

Monga mtsogoleri wotumikira weniweni, ubuse gulu la Mulungu mwa kuwadyetsa Mawu a Mulungu, kulimbikitsa ofooka ndiolobodoka, ndi m'kuwapempherera iwo akudwala ndi osausidwa. Utetezenso nkhosazo ku zolusa (Machitidwe 20:28-31). Kuwonjezera apo, ukhale chitsanzo cha utumiki waumulungu mwa kuwonetsera anthu a Mulungu m'mene angasamalirane wina ndi mzake, komanso m'kuwadandaulira iwo achite chimodzimodzi.[1]

Utsogoleri Wotumikira Dera

Monga Mbusa wa Chipentekoste, dera lanu lachitatu la utsogoleri wotumikira ndi mudzi wanu. Choncho udziwone wekha, usangoti chabe ngati Mbusa wa banja lako ndi mpingo wako, koma monganso Mbusa wa mudzi umene ukukhalamo. Yesu anaphunzitsa kuti ife tikhale "mchere wa dziko lapansi" komanso "kuunika kwa dziko lapansi" (Mateyu 5:13-16). Choncho, udziyike wekha m'gulu la anthu

[1] Kuti mumve zambiri zokhudza kuweta anthu a Mulungu, onani Mutu 24: "Kusamalira Gulu la Nkhosa" ndi Mutu 27: "Kuweta Nkhosa."

a m'mudzi mwako, apempherere iwo, atumikire iwo, ndipo mokhulupilika gawana nawo chikondi cha Khristu.[2]

Yesu anayika muyeso wa utsogoleri wotumikira mu mpingo. Iye anawawuza ophunzira ake, "Pakuti ndithu, Mwana wa Munthu sanadze kudzatumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wake dipo la kwa anthu ambiri" (Marko 10:45). Mbusa wa Chipentekoste atsate m'mapazi a Ambuye wake. Ndipo akhale wosayiwala mawu ake: "Iye amene afuna kukhala woyamba ayenera kukhala wotsiriza, ndi mtumiki wa onse" (Marko 9:35).

[2] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kusamalira dera lanu, onani Mutu 38: "Kutumikira Dera Lanu."

~ Mutu 30 ~

Utsogoleri Wamasomphenya

Atapemphera kwambiri ndi kudzifufuza, Abusa Emmanuel anazindikira kuti Mulungu akuwayitana achoke pa mpingo wabwino ndi wofewa mu mzinda waukulu ndikusamutsa banja lawo kupita ku mudzi mkati mwa nkhalango. Kumeneko, anapitadi kukadzala mipingo. Pokumbukira Abusawa anati, “Ichi chinalichigawo cha mdziko langa chimene kulalikira uthenga wabwino kunali kusanafikitsitse, ndipo kumeneko ndikumene Mulungu amafuna ine ndi banja langa tipite.” Abusa Emmanuel anali wotsimikizika mtima kuti Mulungu anayikiza masomphenyawa mu mtima wawo.

Mzimu Woyera anatsogolera Abusa Emmanuel ku mudzi winawake. Ngakhale deralo linali pabwino, mudziwu umadziwika ngati wozama m’zaufiti. Kuchokera nthawi imene anafika, abusawa ndi mkazi wawo amalandila ziopsezo kuchokera kwa asing’anga a m’deralo. Koma banjali linapirirabe, kulalikira uthenga wabwino kwa onse akumvetsera. Anthu anapulumutsidwa ndi kudzadzidwa ndi Mzimu, ndipo mpingo unayamba kukula ndi kukhwima.

Abusa Emmanuel nthawi zambiri amagawana ndi mamembala awo masomphenya awo a zodzala mipingo yopatsidwa mphamvu ndi Mzimu. Posachedwa, ena anayamba kugwira masomphenyawo, ndipo mu nthawi atsogoleri anayamba kutulukira, amene Abusa Emmanuel anawakonzekeretsera utumiki. Kawiri-kawiri amawatenga atsogoleri otulukirawa kukafalitsa uthenga ndikukhazikitsa mipingo m’dera lozungulira. Kwa zaka zambiri, anazala mipingo

yambiri. Iwo anakonzekeretsanso atumwi nawatumiza kunja kukazala mipingo pakati pa mafuko osafikiridwa cha kumpoto.

Lero, mpingo wa Abusa Emmanuel ukuyenda bwino. Anthu alandira cholinga chawo ndipo adziwona wokha m'masomphenya a abusa awo kuti iwo apitilize kuzala mipingo yatsopano m'chigawocho. Abusa Emmanuel akuwonetseradi chimene ndi tanthauzo lokhala mtsogoleri wamasomphenya.

Kutsogolera mpingo mu utumwi wochitachita, Mbusa wa Chipentekoste adzindikire bwino-bwino cholinga cha Mulungu cha mpingo. Iye akhale ndi masomphenya omveka bwino a m'mene mpingo wawo utengele mbali m'kukwaniritsa cholingacho. Mbusa akaponya masomphenya omveka bwino za kumene mpingoukuyenela upite, anthu amamva kutakasika kutsatira. Koma iye akalephera kuponya masomphenya wotere, mpingo umasautsika (Miyambo 29:18). Mutu uwu ukamba za chosowa cha masomphenya m'kutsogolera gulu lapamalo la okhulupirira.

KUFOTOKOZEDWA KWA UTSOGOLERI WAMASOMPHENYA

Mtsogoleri wachibusa wamasomphenya ndi mwamuna kapena mkazi amene amatsogolera anthu a Mulungu kuchokera pamene ali kupita kumene Mulungu akufuna iwo akakhale. Atsogoleri otsogozedwa ndi Mzimu amakwanitsa kuona m'tsogolo kupambana pano. Iwo amakwanitsa kuwunikira mokhonza nyengo ya pano ya mpingo, kudzindikira mphamvu zake komanso zofooka zake. Ndipo iwo amakwanitsa kuona chimene mpingo ungathe komanso chimene ukhale. Iwo amakwanitsanso kulondoloza njira ya tsogolo la mpingo kukakwaniritsa zolinga zouzilidwa ndi Mulungu. Chomaliza, mtsogoleri wa Chipentekoste wamasomphenya amakwanitsa kutakasa mpingo uyende chitsogolo molimba mtima m'kukwaniritsa zolingazo.

MAKHALIDWE A ATSOGOLERI AMASOMPHENYA

Tiyeni tione makhalidwe asanu ndi atatu a atsogoleri amasomphenya monga awonetseredwa m'Malemba:

Otsogozedwa ndi Mzimu

Choyamaba, mtsogoleri wamasomphenya weniweni amakhala wotsogozedwa ndi Mzimu. Mbusa wa Chipentekoste asanatsogolere mpingo wake m'zolinga za Mulungu, iye yekha akhale odzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndi

wokwanitsa kutsatira utsogoleri wa Mzimuyo (Agal. 5:25). Iye akhale wofunitsitsa kusiya zolinga zake ndikutsatira zolinga za Mulungu mwachidwi.

Odzadzidwa ndi Chikhulupiriro

Chachiwiri, atsogoleri amasomphenya amakhala odzadzidwa ndi chikhulupiriro. Iwo ali ndi kuthekera kokhulupirira Mulungu ndi kumudalira Iye akakumana ndi nyengo zovuta (Ahebri 11:1-37).

Owona

Chachitatu, atsogoleri amasomphenya amapereka chitsanzo chenicheni kuti mpingo utsatire (Afilipi 3:17). Ali ndi mbiri yokhulupirika ya utumiki wotsimikiziridwa kuti ali ndi ufulu wotsogolera mpingo. Iwo amasonyezadi munthu m'mene Mulungu amayembekezera mpingo kuchitapo kanthu ku masomphenya ake operekedwa ndi Mulungu.

Oganizira Zamtsogolo

Chachinayi, atsogoleri amasomphenya ndi amtsogolo. Maganizo awo amakhala okhazikika osati pa zomwe adakwaniritsa dzulo, koma pa mwayi wamawa. Paulo anapereka chitsanzo cha khalidwe limeneli pamene anachitira umboni, "Chinthu chimodzi ndichichita: poiwaladi zam'mbuyo ndi kutambalitsira zam'tsogolo (Afilipi 3:13)

Aulosi ndi Ochita

Chachisanu, atsogoleri amasomphenya ali, panthawi imodzimodzi, aulosi ndi ochita. Iwo ndi aulosi chifukwa amaona zomwe zingatheke. Amakhala ochita kapena othandiza chifukwa amazindikira zoyenera kuchita kuti akwaniritse cholingacho. Poganizira zam'tsogolo, mtsogoleri wamasomphenya ayenera kukhala wokhoza kutsogolera mpingo mwachidwi pamavuto omwe alipo.

Odalirika

Chachisanu ndi chimodzi, atsogoleri amasomphenya ndi odalirika. Ali ndi mbiri yotsimikizika yodalirika m'mbuyomu. Chifukwa cha zimenezi, anthu a Mulungu amakhala ofunitsitsa kuwatsatira m'tsogolo atsogoleri wotere.

Wopangitsa

Chachisanu ndi chiwiri, atsogoleri amasomphenya ndi wopangitsa kapena ali ndi chikoka. Iwo ali ndi mphamvu yopatsidwa ndi Mulungu yosonkhezera ena kuchitapo kanthu. Iwo ali ndi mphatso ndi maluso ofunikira kuti alimbikitse malingaliro, zosankha, ndi zochita za ena.

Olimba Mtima

Pomaliza, atsogoleri amasomphenya ali olimba mtima. Iwo ali olimba mtima kuti apite ku tsogolo lomwe panthawiyi sakulidziwa bwino. Pamene Mbusa Emmauel adasiya mzinda waukulu umene anauzolowera komanso wabwino, sanadziwe chimene chinali patsogolo pake. Komabe, iye molimba mtima anatsogolera banja lake kumalo osadziwika, akudalira kuti Mulungu adzawapatsa zosowa zawo.

ZITSANZO ZA ATSOGOLERI AMASOMPHENYA

M'njira zambiri, Baibulo ndi nkhani ya amuna ndi akazi amene Mulungu anawadzutsa ndi kuwadzoza monga atsogoleri amasomphenya. Atsogoleriwa akupereka chitsanzo cha utsogoleri womwe tatchulawu. Amuna asanu ndi m'modzi otsatirawa ndi atsogoleriwo:

Abrahamu: Masomphenya Odzala ndi Chikhulupiriro

Abrahamu anali mtsogoleri wamasomphenya wodzadzidwa ndi chikhulupiriro. Ndi chikhulupiriro iye anayang'ana za mtsogolo ndipo anaona "mzinda wokhala nao maziko, mmisiri wake ndi womanga wake ndiye Mulungu" (Ahebri 11:10). Ndiye, mwa chikhulupiriro, iye anatsogolera banja lake ku dziko losadziwika, akukhulupirira kuti Mulungu adzakwaniritsa lonjezo lake kwa iye (Ahebri 11:8). Pochita izi, anakhulupirira "Tate wa onse okhulupirira" (Aroma 4:11).

Yosefe: Kuzindikira Mwaulosi

Yosefe anatsogolera mwachidziwitso chaulosi. Mulungu anam'patsa kuzindikira tanthauzo la loto la Farao (Genesis 41:15-24). Kenako Yosefe anapereka malangizo othandiza kwa mfumuyo pa zimene inayenera kuchita ndi ulosi umenewu (ndime 25-36). Chifukwa cha zimenezi, ambiri anapulumutsidwa

ku njala. Farao anaona Mzimu wa Mulungu mwa Yosefe ndipo anamukweza pa udindo wapamwamba wa utsogoleri, wachiwiri kwa Farao yekha (ndime 37-44).

Yoswa ndi Kalebe: Masomphenya Olimba Mtima

Masomphenya olimba mtima a Yoswa ndi Kalebe anawathandiza kulimbikira m'chikhulupiriro pamene ena anali kuchoka chifukwa cha mantha (Numeri 14:6-9). M'malo mogonja kumantha awo, Yoswa ndi Kalebe anasankha kukhulupirira Mulungu. Pamene anthu anakana kutsatira chitsogozo chawo, iwo anakhalabe okhulupirika ku kudzipereka kwawo ndi kusunga masomphenyawo amoyo kwa zaka makumi anayi, kukonzekeretsa m'badwo wotsatira kulowa m'Dziko Lolonjezedwa.

Nehemiya: Kukhala Pamodzi m'Cholinga

Nehemiya anatsogolera anthu a Mulungu kukamanganso malinga a Yerusalemu ndi cholinga chimodzi. Iye anachita zimenezi ngakhale kuti ankatsutsidwa kwambiri. Anachilikizidwa ndi masomphenya ake a zimene zikanatheka ngati anthu a Mulungu akanaikabe maganizo awo pa ntchito yopatsidwa ndi Mulungu.

Hagai: Kusadzikonda

Mtima wodzipereka wa Hagai unasonkhezera anthu a Mulungu kusiya kudzikonda ndi kuika ntchito ya Mulungu patsogolo. Iye adawapempha kuti asiye kuyika chuma chawo chonse pomanga nyumba zawo. M'malo mwake, anafunika kudzipereka okha pomanga nyumba ya Mulungu. Mneneriyo anauza anthu a Mulungu kuti, ngati angayende limodzi ndi cholinga chogwirizana, ntchitoyo idzamalizidwa.

Yesu: Mathero a Chitsanzo Chathu

Ambuye wathu Yesu Khristu ndiye chitsanzo chopambana cha mtsogoleri wamasomphenya. Iye ankamvetsa bwino lomwe chifukwa chimene anabwerera, kumene ankapita, ndiponso zimene ayenera kuchita kuti akafikire kumeneko. Iye ndi chitsanzo chabwino cha munthu amene adawona njira yakutsogolo ndikudzipereka kwathunthu kutsatira (onani Ahebri 12:2). Kenako anasankha, kuphunzitsa, ndi kulimbikitsa ena kuti agwirizane naye pa ntchitoyo.

Paulo: Masomphenya a Utumwi

Wachiwiri kwa Yesu, Paulo anali mtsogoleri wamkulu wa utumwi wa nthawi zonse. Paulo anatsogozedwa ndi masomphenya akumwamba kukatengera uthenga wabwino kwa Amitundu. Iye anapereka masomphenya ake kwa ena, ndipo anawapatsa chitsanzo cha kulalikira, kudzala mipingo, ndi utumwi. Chakumapeto kwa utumiki wake, Paulo anatha kuchitira umboni kuti, "Sindinakhala ine wosamvera masomphenya a kumwamba" (Mach. 26:19).

MPHAMVU ZA UTSOGOLERI

Kuti mukhale mtsogoleri weniweni wamasomphenya, mukufunika kumvetsetsa kwamphamvu za utsogoleri. Ndipo mukufunika kumvetsetsa bwino momwe utsogoleri wamasomphenya umawonekera muzochita zenizeni.

Utumwi ndi Masomphenya

Choyamba, muyenera kumvetsetsa mgwirizano pakati pa utumwi ndi masomphenya. Mu ufumu wa Mulungu, masomphenya amakula kuchokera mu utumwi, osati mosiyana. Cholinga cha Mpingo chinasankhidwa kale ndi Mulungu. Cholinga cha Mulungu, chomwe nthawi zina chimatchedwa *missio Dei,* ndicho kuombola ndikuyitanira kwa Iye yekha anthu ochokera ku fuko lililonse, chinenero chilichonse, ndi mtundu ulionse pa dziko lapansi Khristu asanabwere. Yesu analankhula zimenezi mu Kutuma Kwake Kwakukulu: "Pitani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera, ndi kuwaphunzitsa kusunga zonse zimene ndinakulamulirani inu" (Mateyu 28:18-20; onaninso Marko 16:15-18; Luka 24:49; Yohane 20:21; Machitidwe 1:8). Mpingo ulipo kuti ukakwaniritse cholinga cha Mulungu.[1]

Khristu walamula Mbusa aliyense wa Chipentekoste ndi mpingo kutenga nawo mbali mokwanira mu utumiki wake. Iye wayika kuti mpingo uliwonse ukhale mpingo wautumwi. Chifukwa chake, mpingowo uyenera kuchitapo kanthu mu ulaliki, kuphunzitsa, ndi kudzala mipingo. Kuphatikiza apo, mpingo uliwonse wa Chipentekoste uyenera kukulitsa masomphenya odzutsa ndi kutumiza atumwi

[1] Kuti mudziwe zambiri za masomphenya a utumwi, onani Mutu 31: "Utsogoleri wa Utumwi."

ndi antchito ena achikhristu. Mipingoyi iyeneranso kudzipereka kuthandiza ogwira ntchitowa ndi mapemphero ndi ndalama.[2]

Masomphenya akulankhula za malingaliro odzozedwa ndi Mzimu a mpingo pa ntchito yawo pokwaniritsa cholinga cha Mulungu. Ndi uneneri m'chilengedwe, osayang'ana ntchito za lero zokha komanso mwayi wamawa. Masomphenya amalumikizitsa zomwe mpingo uli lero ndi zomwe Mulungu akufuna kuti ukhale mawa. Ndi chifaniziro chamaganizo chouzilidwa ndi Mzimu cha chimene mpingo, mothandizidwa ndi Mulungu,ungakhale.

Pamene inu ndi mpingo umene mumautsogolera muyamba kuvomereza utumwi wa Mulungu, Mulungu adzakupatsani masomphenya a chimene Iye akufuna kuti mukwaniritse. Masomphenya ouzilidwa ndi Mulungu amenewa nthawi zonse adzagwiriza ndi cholinga cha Mulungu, monga tafotokozerapamwambapo. Ichi ndi chifukwa chake ndikofunika kuti mukhale ndi chidziwitso chomveka bwino cha utumwi wa Mulungu ndi momwe utumwiwo ukugwirizanirana ndi cholinga cha utumwi cha mpingo. kuchokera mu utumwi kumabwera masomphenya, kuchokera mu masomphenya kumabwera zolinga, ndipo kuchokera mu zolinga kumabwera zochita.

Kukulitsa Masomphenya

Mofanana ndi mmene munda umafunika kulima kuti ubereke mbewu zabwino, masomphenya ayenera kukulitsidwa kuti atulutse njira zouzilidwa ndi Mulungu. Mungathe kukulitsa masomphenya mu mtima mwanu komanso mu mpingo umene mukubusawo mukugwiritsa ntchito njira zitatu izi:

1. Kuwerenga Baibulo Mwakuganizira. Choyamba, mukhonza kukulitsa masomphenya mumtima mwanu mwa kuwerenga Baibulo Baibulo mosinkhasinkha kapena mwakuganizira. Mutha kuwerenga mwapemphero nkhani za atsogoleri akulu m'Malemba omwe Mulungu adawagwiritsa nntchito kupititsa patsogolo ufumu wake. Pamene mukuwerenga, dzifunseni mafunso otsatirawa:

- Kodi Mulungu Anaika masomphenya otani mu mtima mwa mtsogoleri ameneyu?
- Kodi mtsogoleriyu anadziwa bwanji masomphenyawo?
- Kodi anachita chiyani kuti akwaniritse masomphenyawo?

[2] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kulimbikitsa mpingo wanu ku utumwi, onani Mutu 40: "Kukhazikitsa Dongosolo la Utumwi wa Mpingo."

- Kodi Mulungu akunena chiyani kwa ine kudzera munkhaniyi?

Lembani mayankho anu mu kope ndikusinkhasinkha mwapemphero mu mtima mwanu. M'kupita kwa nthawi, mungafune kuyambitsa maulaliki ochokera m'malingaliro amenewa ndi kuwagawira ku mpingo wanu. Mwanjira imeneyi, inu ndi anthu anu mukhonza kukula limodzi mu kumvetsa kwanu kwa utumiki wa Mulungu ndi udindo wa mpingo wanu pokwaniritsa utumikiwo.

2. Kudikirira pa Mulungu. Chachiwiri, mukhoza kukulitsa masomphenya mumtima mwanu mwa kuyembekezera Mulungu m'pemphero. Yambani ndi kuyandikira kwa Iye kudzera mu chiyamiko chowonadi ndi matamando (Yakobo 4:8). Mukuzindikira kupezeka kwa Mulungu, muyenera kupemphera kuti, "Ambuye ndiwonetseni chifuniro chanu. Ndiloleni ndiwone mtima wanu." Muyenera kukhala pamaso pa Mulungu, kupemphera mu Mzimu ndikumvera mawu ake (Aroma 8:26-27; Aefeso 6:18).

Pamene mupemphera motero, mukhale tcheru pamalingaliro amene akubwera pafupipafupi kapena izo zomwe Mzimu Woyera akuika mtima mwanu. Pakupita kwanthawi malingaliro amenewo adzakhala akukukankha mkati mwako kuti uchitepo kanthu. Pamapeto pake athe kukhala katundu mu mtima mwako. Pokhala katundu, zidzabweretsa kumvetsetsa kwakuya kwa komwe Mulungu akutsogolera mpingo (Yesaya 30:21). Mudzafunikanso kutsogolera mpingo kunthawi yakufunafuna chitsogozo kuchokera kwa Mulungu.

3. Kuwona Chosowa. Pomaliza, mutha kukulitsa masomphenya poyang'ana mwapemphero zosowa za anthu amdera lanu kapena malo ena osankhidwa (fanizilani Yohane 4:35). Pamene muyang'ana, pemphani kwa Mulungu akupatseni nzeru, pemphani kuti, "Ambuye, ndithandizeni kuona zosowa za mkati mwa anthu" (fanizilani 2 Akorinto 4:18). Pamene muyang'ana, pemphani Mulungu kuti akupatseni chidziwitso. Muyenera kupempheranso kuti, "Ambuye, ndi ziti mwa zosowa izi zomwe mukufuna kuti mpingo wathu ukwaniritse?" Mukamaliza kupemphera, khalani chete ndipo mvetserani kuyankha kwa Mulungu.

Udindo wa Mzimu Woyera

Tikukhala m'masiku otsiriza, pamene Mulungu akutsanulira Mzimu wake pa anthu onse (Mach. 2:17-18). Mulungu watipatsa Mzimu wake kuti atipatse mphamvu ndi kutitsogolera pa ntchito. Monga mtsogoleri weniweni wa

Chipentekoste, muyenera kukhala odalira utsogoleri wa Mzimu nthawi zonse. Ngakhale utsogoleri wamakono ndi njira zakukulira kwa mipingo zili ndi malo ake, musamadalire kwambiri njira zomwe anthu amaziganizira. Monga mtsogoleri wauzimu wamasomphenya, muyenera kufunafuna chitsogozo cha Mzimu nthawi zonse ndi kutsatira chitsogozo chake, mukukumbukira mawu a mneneri akuti, "si mphamvu, kapena ndi nkhondo, koma ndi Mzimu wanga, atero Yehova Wamphamvuzonse" (Zekariya 4:6).

Kuponya Masomphenya

Ngakhale kuti masomphenya aumwini ndi ofunika, sikokwanira kuti mukhale ndi masomphenya ndikusunga nokha. Muyenera kutha kufotokozera masomphenya ku mpingo. Ndipo muyenera kuzichita m'njira yolimbikitsa anthu a Mulungu kutsatira. Njirayi imatchedwa kuponya masomphenya. Ntchito yaikulu ya Yesu ndi ophunzira ake inali yoponya masomphenya. Iye nthawi zonse ankagawana nawo masomphenya ake ndi kuwabetchera kuti amutsatire Iye.Momwemonso, ndikofunikira kuti mufotokoze masomphenya anu ku mpingo ndikuyitanitsa mamembala kuti "atsatire chitsanzo [chanu], monga mutsata chitsanzo cha Khristu" (1 Ako. 11:1).

Kuti izi zitheke, masomphenyawo ayenera kulimbikitsa malingaliro a anthu. Ayenera kukhala wovuta koma wotheka. M'mawu ena, masomphenyawo asakhale aakulu kwambiri mpaka kuphwanya mphamvu za anthu. Komanso sayenera kukhala aang'ono kwambiri mpaka kulephela kuwalimbikitsa. Ngati masomphenyawo ndi aakulu kwambiri moti anthu sangawagwire, Mbusayo ayenera kuwachepetsa m'zidutswa zing'onozing'ono, ndi zolinga zanthawi yochepa komanso za nthawi yayitali.

Nthawi zina ndi bwino kutulutsa masomphenyawo pang'onopang'ono. Choyamba, mungafune kugawana masomphenyawo ndi mkazi kapena mwamuna wanu kapena gulu lamkati la anzanu ndi atsogoleri odalirika. Mutha kukambirana, kupemphera, ndi kulandira umboni kuchokera kwa Mzimu kuti mupitirize.Kenako, mudzafuna kugawana masomphenyawo ndi a komiti ndi ogwira ntchito pa mpingo, kuti apeze mwayi wawo. Zimatengera gulu kuti masomphenya akwaniritsidwe. Chifukwa chake ndikofunika kuti mamembala onse a gulu akhale nawo.

Nthawi ikakwana yogawana masomphenya ndi mpingo, mutha kukonzekera "Lamulungu la Masomphenya." Chochitikachi chidzakupatsani inu nsanja

yofotokozera momveka bwino masomphenyawo kwa anthu. Muyenera kulankhula pafupipafupi za masomphenyawo ndikulalikira mokhazikika. Njira imeneyi idzathandiza kuika masomphenya m'mitima ya anthu.

Komanso, muyenera kuyesetsa kuonetsetsa kuti mpingo wonse ukuyenda limodzi kukwaniritsa masomphenyawo. Muyenera kulimbikitsa aliyense kupereka, kupita, kugwira ntchito, kutumikira, ndi kudzipereka kuti awone masomphenyawo akukwaniritsidwa. M'kupita kwa nthawi, mungafune kuitana anthu ena kuti apereke umboni wa mmene masomphenyawo akukwaniritsidwira. Maumboni amenewa athandiza kulimbikitsa anthu komanso kuti mpingo uziyenda bwino.

Kugonjetsa Zopinga

Musadabwe pamene kukhazikitsidwa kwa masomphenyawo kuyesedwa. Mpingo uliwonse umene umafuna kutsata masomphenya a Mulungu udzakumana ndi zopinga ndi kutsutsidwa ndi ziwanda. Paulo analembera Akhristu a ku Tesalonika kuti, "Chifukwa tinafuna kudza kwa inu…koma Satana anatiletsa" (1 Ate. 2:18).

Kutsutsidwa koteroko sikungalempheretse kupita patsogolo kwa mpingo. Zidzakhala zofunikira, komabe, kuti inu ndi mpingo mugwiritsire ntchito masomphenyawo. Ngati mukhalabe olunjika pa masomphenya amene Mulungu wakupatsani, adzakwaniritsidwa. Yesu analonjeza kuti, "Ndidzakhazika mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaugonjetsa uwo" (Mat. 16:18).

Munkhani yomwe yanenedwa kumayambiriro kwa mutu uwu, Mbusa Emmanuel anali wokhulupirika ku masomphenya amene Mulungu anamupatsa. Kupyolera mu kumvera ndi chikhulupiriro, iye anapirira mpaka masomphenyawo anakwaniritsidwa. N'chimodzimodzinso kwa inu. Ngati mupeza masomphenya a Mulungu a mpingo wanu, ndipo ngati mungapyole mu nyengozamavuto, inunso mutha kuwona kukwaniritsidwa kwa masomphenya anu. Mungathe kunena molimbika mtima lonjezo la Mulungu kwa Habakuku: "Pakuti masomphenyawo alindira nyengo yoikidwiratu…akachedwa uwalindirire; popeza afika ndithu, osazengereza" (Habakuku 2:3).

~ Mutu 31 ~

Utsogoleri wa Utumwi

Tsiku lina Yesu anali kuyenda m'mbali mwa Nyanja ya Galileya. Kumeneko anakumana ndi Petro ndi Andireya akuponyamakoka awo m'nyanja. Iye anati kwa iwo: "Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu." Baibulo limati: "Ndipo pomwepo anasiya makoka ao, namtsata Iye" (Marko 1:16-18). Anthu mwachibadwidwe amakopeka ndi atsogoleri omwe ali ndi chizindikiro champhamvu cha cholinga. Anthuwo Mwachibadwa amasunthika kuwatsatira atsogoleri oterewa, monga momwe Petro ndi Andreya anasunthika kutsatira Yesu.

Mutu uwu ufotokoza za udindo wa Mbusa wa Chipentekoste ngati mtsogoleri wa utumwi. Udzakambirana udindo wao wotsogolera mipingo yawo kuti igwire ntchito ya Mulungu pa dziko lapansi. Udzakambirananso momwe angalimbikitsire ena kuti awatsatire panjira yayikuluyi.

MBUSA WA UTUMWI

Yesu mwiniyo anali mtsogoleri wa utumwi, ndipo Iye akuitana Mbusa wa Chipentekoste kuti akhale chimodzimodzi. Akuyang'ana amuna ndi akazi okhala ndi mzimu wofunikira, kudzipereka, ndi chikhulupiriro kuti atsogolere anthu ake mu utumiki (onani 2 Mbiri 16:9).

Makhalidwe Ofunikira

Atsogoleri autumwi amadziwa kumene akupita, ndipo amadziwa kuti akafika bwanji kumene akupitako. Chifukwa chake, amatha kulimbikitsa ena kuti agwirizane nawo paulendowu. Abusa autumwi ali ndi makhalidwe itatu yofunikira:

1. Kumvetsetsa. Abusa autumwi amamvetsetsa ntchito ya Mulungu. Amazindikira kuti ndi Mulungu wautumwi ndipo ali pa ntchito yowombola ndi kuitana kwa Iye yekha anthu ochokera m'mitundu yonse padziko lapansi (Mateyu 24:14; Chivumbulutso 5:9; 7:9). Lingaliro limeneli limadziwika kuti *missio Dei,* lomwe ndi Chilatini kutanthauza "cholinga cha Mulungu." Mbusa wautumwiyo amamvetsetsa kuti mpingo ulipo kuti ukwaniritse ntchito ya Mulungu padziko lapansi. Iye amamvetsetsanso kuti imodzi mwa ntchito zawo zazikulu monga Mbusa ndi kulimbikitsa mpingo kuti ukwaniritse cholinga cha Mulungu.[1]

2. Kudzipereka. Kupitilira kumvetsetsa ntchito ya Mulungu, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kudzipereka kutsogolera mpingo wake kuti utenge nawo gawo mokwanira pakukwaniritsa ntchitoyo mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Ayenera kukhala wokonzeka kuchita chilichonse chimene angathe kuti akwaniritse udindo waukulu umenewu.

3. Luso. Pomaliza, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kudzipereka kukulitsa malingaliro ndi maluso ofunikira kulimbikitsa mpingo kuchita utumwi wa Mulungu. Mbusa weniweni wa Chipentekoste amazindikira kuti, kukhoza kwake mu utumiki kumachokera kwa Mulungu kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera (Machitidwe 1:8; 2 Akorinto 3:5-6).

Chitsanzo cha Yesu

Yesu anali mtsogoleri wotsimikizika wa utumwi. Iye anamvetsa bwino lomwe chifukwa chimene anadzera padziko lapansi. Iyeanalengeza kuti, "Pakuti Mwana wa munthu anadza kudzafunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho" (Luka 19:10). Kumalo ena, ananena kuti: "Ndinatsika Kumwamba, osati kudzachita chifuniro changa, koma kudzachita chifuniro cha Iye amene ananditumaIne"

[1] Kuti mudziwe zambiri za utumwi wa Mulungu, onani buku la Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Chiphunzitso cha M'baibulo cha Utumwi,* lolembedwa ndi Paul York, lopezeka kuchokera ku Africa Theological Training Service (ATTS), www.africaatts.org.

(Yohane 6:38). Nthawi ina Yesu anatchula ntchito yake monga "chakudya" chake (Yohane 4:34). Monga momwe chakudya chimalimbitsira thupi ndi kupatsa mphamvu, Yesu nayenso analimbikitsidwa ndi kudyetsedwa mwa kuchita chifuniro cha Atate wake. Kudzipereka kumeneku kunamufikitsa pa mtanda (Mateyu 20:28).

Asanabwerere kumwamba, Yesu anapereka utumwi ndi utumiki wake ku mpingo wake. Iye anauza ophunzira ake kuti: "Monga Atate wandituma Ine, Inenso ndituma inu" (Yohane 20:21). Monga momwe Yesu adapezera ntchito yake mu chifuniro cha Atate wake, Mbusa wa Chipentekoste amapeza ntchito yake mu chifuniro cha Khristu. Ndipo monga momwe kudzipereka kwa Yesu pakuchita chifuniro cha Atate wake kunamuchilikiza mu utumiki wake, momwemonso kudzachilikiza Mbusa wa Chipentekoste mu utumiki wake (Mateyu 26:36-44; 28:19-20; Yohane 14:16).

Kukhala Musanachite

Monga Mbusa wa Chipentekoste ndikofunikira kuti mumvetsetse kuti utsogoleri wa utumwi uli kwambiri m'kukhala kuposa m'kuchita. Kumbukirani, Yesu analonjeza Petro ndi Andreya kuti: "Nditsateni ine, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu." (Marko 1:17). Potsatira Yesu ndi kudzazidwa ndi Mzimu wake, umunthu weniweni wa ophunzirawo ukanasandulika. Iwo *adzakhala* ngati Mphunzitsi wawo (Luka 6:40; Machitidwe 4:13).

Sikuti Mzimu adzangowathandiza kuti atumikire ndi mphamvu, adzapereka kwa iwo chilakolako cha Khristu cha kututa. Choncho Mzimu Woyera adzawasintha iwo kuti khama lawo, zokhumba zawo, ndi luso lawo zikhale pansi pa ulamuliro wa Khristu. Iwo adzagwirizana ndi Khristu pokwaniritsa ntchito ya chiombolo ya Mulungu. Ubatizo wa Mzimu Woyera ukhonza kupanga maziko a utumwi wawo wamtsogolo (Machitidwe 1:4-5).[2]

Chimodzimodzinso masiku ano. Ngati tingalore Mzimu wa Mulungu kutidzadza ndi kugwira ntchito mwa ife, adzatisintha kukhala chifaniziro cha

[2] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kubatizidwa ndi Mzimu Woyera, onani Mutu 10, 11, ndi 20.

Khristu (onani 2 Akorinto 3:18). Ndipo adzatipatsanso chilakolako chotuta chomwe chinali mwa Yesu.

Kukhala Wautumwi

Ambuye Yesu anaitana amuna ndi akazi kuti amtsate Iye ndi kupitiriza ntchito imene anaiyamba. Kenako Anaika nthawi yake ndi mphamvu zake powaphunzitsa ndi kuwaumba kukhala atsogoleri autumwi. Njira imodzi imene Yesu anachitira inali mwa kuwatumiza ku maulendo aafupi a utumwi. Anawalangiza, kuwakonzekeretsa, kenako anawatumiza (Luka 9:1-6; 10:1-16). Pamene adabwerera iwo, Iye adakhala nawo pansi nakambirana za ntchito yawo (Luka 10: 17-20).

Ophunzira khumi ndi awiri a Yesu sanali obadwa ndi utsogoleri. Iwo sanalinso okonda utumwi mwachibadwa. Anali anthu wamba ogwira ntchito. Komabe, iwo analolera kuika moyo wawo m'manja mwa Yesu kuti aumbidwe ndi Iye. Kupyolera m'moyo ndi chiphunzitso chake, Yesu anapereka kwa iwo masomphenya ake a dziko lonse lapansi. Iye anawalamula kuti: "Pitani mukaphunzitse anthu a mitundu yonse kuti akhale ophunzira anga" (Mateyu 28:19). Iye analimbikiranso kuti iwo apatsidwe mphamvu ndi Mzimu Woyera, monga momwe Iye anachitira (Luka 4:18-19; Machitidwe 1:8).

Kamodzi mwa mikumano yoyambirira ya Petro ndi Ambuye, iye anadzichotseratu yekha kukhala mmodzi wa atsogoleri. Iye anapempha Yesu kuti: "Muchoke kwa ine, Ambuye, chifukwa ndine munthu wochimwa!" (Luka 5:8). Petro ankaziona ngati wosayenera chifukwa cha munthu amene anali. Komabe, Yesu ankaziwa chimene Petro angachite. Chotero Iye anayankha Petro kuti, "Usaope, kuyambira tsopano udzakhala msodzi wa anthu" (ndime 10). Pamene Petro ankayenda ndi Yesu, anasandulika kukhala mtsogoleri wamphamvu wautumwi amene timawerenga za m'buku la Machitidwe.

Baibulo limati, "Yesu anasankha atumwi khumi ndi awiri kuti akakhale ndi Iye ndi kuti akawatume kukalalikira" Marko 3:14). Mwakukhala ndi Yesu, kumvetsera zimene anali kuphunzitsa, ndi kuona zochita zake, ophunzirawo anakhala ngati Ambuye wawo. Yesu anawaumba kukhala atsogoleri autumwi, aliyense m'njira yapadera kuti agwire ntchito yapadera. Chifukwa anachita zimenezi, Mpingo umene anauyambitsa ukupitirirabe mpaka lero. Monga abusa ofunitsitsa a Chipentekoste, tingachite bwino kukhala ndi nthawi ndi atsogoleri

autumwi ogwira mtima. Tikamatsatira kwambiri Yesu, n'kumayanjana ndi anthu amene amachita zofanana ndi zimenezi, tidzasintha.

Ndodo ya utsogoleri yaperekedwa kwa ife. Ifenso tiyenera kuyesetsa kukhala atsogoleri owona zautumwi. Mofanana ndi Yesu ndi atumwi, tiyenera kuyesetsa kukulitsa ena. Paulo analembera Timoteo kuti, "Ndipo iwe, mwana wanga, limbika m'chisomo cha mwa Khristu Yesu. Ndipo zimene wazimva kwai ne mwa mboni zambiri, zomwezo uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso" (2 Timoteo 2:1-2).

CHIKHUMBO CHAUTUMWI

Zochita zautumwi zimatuluka chifukwa cha chikhumbo chautumwi kapena Khama lautumwi. Chikhumbo ndi kufunakwamphamvu kofuna kukwaniritsa chinthu chofunika kwambiri. Wamasalimo analankhula za chikhumbo cha Mulungu cha Mwana wake-ndi mitundu. Atate anati kwa Mwanayo, "Undifunse, ndipo ndidzakuyesa amitundu cholowa chako, malekezero a dziko lapansi likhale lako" (Masalimo 2:8). Monga ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, tingagwirizane ndi Mwana m'pemphero lautumwi limeneli. Kuchita zimenezi kudzatithandiza kukhala ndi chikhumbo champhamvu cha kuona mabwenzi ndi anansi athu akubwera kwa Yesu. Panthawi imodzimodziyo, kudzachititsa mwa ife kukhala ndi chikhumbo chofuna kuona mafuko akufikiridwa ndi uthenga wabwino wa chipulumutso mwa Khristu.

Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kupanga chikhumbokhumbo cha Mulungu kukhala chanu. Izi n'zimene Abrahamu anachita. Ngakhale kuti anali wokalamba komanso wopanda mwana, Mulungu anamuuza kuti, "Tayang'anatu kumwamba, uwerenge nyenyezi…Zoterezo zidzakhala mbewu zako" (Gen. 15:5). Abrahamu anakhulupirira lonjezo la Mulungu ndipo anagawana zokhumba zake. Chifukwa cha kumvera kwake, anakhala tate wa onse okhulupirira (Aroma 4:11). Pemphani Mulungu kuti akupatseni chikhumbo chake pamitundu. Ndiye lolani chilakolako ichi chikulimbikitseni kulimbikitsa mpingo wanu kutenga nawo mbali mu utumwi wa Mulungu.

ZOCHITA ZAUTUMWI

Ngakhale kufunitsitsa kwautumwi kuli kofunika, kokha sikukwanira. Monga Mbusa wa Chipentekoste, muyenera kuyesetsa kusintha zokhumba kukhala zenizeni. Paulo ndi chitsanzo cha choonadi ichi. Iye anali ndi chikhumbokhumbo

chofuna kuona amitundu akutembenukira kwa Khristu (Mach. 22:21; Aroma 10:1). Chikhumbo chimenechi chinamukakamiza iye kugwira ntchito molimbika kaamba ka chipulumutso chawo. Iye anachitira umboni kuti, "Ndinagwira ntchito molimbika koposa onsewo-koma si ine ayi, koma chisomo cha Mulungu chakukhala ndi ine" (1 Ako. 15:10). Momwemonso, nanunso muyenera kusintha chikhumbo chanuchautumwi kukhala ntchito yautumwi. Muyenera kukulitsa mpingo wanu kukhala mpingo wautumwi weniweni.

Kukhazikitsa Masomphenya Autumwi

Udindo waukulu wa Mbusa aliyense wa Chipentekostendikukhazikitsa chilakolako cha otayika m'mitima ya anthu a Mulungu. Anthuwo ayenera kuzindikira kwambiri kutayika kwa anthu amene ali kunja kwa mpingo wawo. Ayeneranso kuzindikira kutayika kwa anthu osafikiridwawo okhala m'malo osafikiridwa mu Afirika yense ndi kuzungulira dziko lonse lapansi. Kuti zimenezi zitheke, muyenera kulalikira, kuphunzitsa, ndi utumiki wachitsanzo pamaso pa mpingo wanu. Ndipo mudzafunika kupirira mpakamembala aliyense wa mpingo amvetse udindo wake wochita nawo *missio Dei.*

Masomphenya a utumwi amaikidwa m'mitima ya anthu a Mulungu m'njira ziwiri: mwa Mzimu wa Mulungu ndi mwa Mawu a Mulungu. Zinatengera kusuntha kwamphamvu kwa Mzimu ndi mawu anthawi yake ochokera kwa Ambuye kuti asinthe malingaliro a Petro okhudza amitundu (Mach. 10:9-16, 19-20). Monga mtsogoleri wautumwi, muyenera kuwonetsetsa kuti mu mpingo wanu mulinso chimodzimodzi. Muyenera kuwonetsetsa kuti Mzimu akuyenda mwamphamvu mu mautumiki anu, ndipo muyenera kuyesetsa kuona kuti membala aliyense wadzazidwa ndi Mzimu. Nthawi zonse, muyenera kuwafotokozera anthu chifukwa chake Mzimu wa Mulungu akuyenda. Monga Mzimu wa utumwi wa Mulungu, Iye akuwakonzekeretsa kutenga nawo mbali mu utumiki wa Mulungu.

Komanso, muyenera kuphunzitsa anthu zimene Baibulo limanena zokhudza utumwi wa Mulungu. Ndipo muyenera kuwawonetsa momwe ayenera kudzipereka okha kupempherera mwachangu otayika, kupereka mowolowa manja ku utumwi, ndikugawana mokhulupirika uthenga wabwino ndi iwo omwe ali nawo pafupi. Pomaliza, muyenera kuwabetchera kuti adzipereke ku ntchito ya Mulungu.

Monga mtsogoleri weniweni wa utumwi, muyenera kutsogolera mpingo wanu kuchoka kudziko longoganizira za inu nokha, kukhala kudziko longoganizira za ena, kuchoka pa zofuna zawo ndi kuyika maganizo awo pa zosowa za dziko lotayika lozungulira iwo. Ulendo wa utumwiwu udzafunika kukhala ndi cholinga champhamvu kumbali yanu. Zidzafunikanso kuti musinthe madongosolo a mpingo wanu ndi kusintha kwa cholinga ndi zomwe zili pamisonkhano yanu.

Kugawana Nkhani Zautumwi

Njira imodzi yotsimikizika yomwe mungapangire mpingo wokonda utumwi ndi kugawana nkhani zautumwi ndi anthu anu. Mungachite zimenezi mwa kuphatikiza nkhanizi mu ulaliki wanu ndi kuphunzitsa. Zambiri mwa nkhani zimenezi zimapezeka m'Baibulo. Nkhani ya Yesu ndi nkhani yautumwi yopambana kwambiri imene inanenedwapo. Ndipo m'buku la Machitidwe muli nkhani zambiri zosangalatsa za utumwi. Mukhozanso kupeza nkhani powerenga mabuku a atumwi komanso kumvetsera atumwi akulankhula. Komanso, musazengereze kuuzako mpingo nkhani zanu zautumwi.

Kukonzekera Utumiki Wautumwi

Mudzafunanso nthawi zonse kukonza atumwi kuti alankhule ndi mpingo wanu. Mukhonza kuwaitana kuti abwere ku utumwi wapadera kapena kumapeto kwa sabata yodziwitsa za utumwi. Atumwi akabwera, musaiwale kulipira ndalama zoyendera. Ndipo mudzafunika kupatsa mpingo mwawi wa kutengapo mbali mu utumiki wa atumwi mwa kulandira chopereka chowolowa manja kaamba kaiwo. Mpingo uyeneranso kuganizira njira zoimira ndi m'tumwiyo mosalekeza.[3]

Kupanga "Mabwalo a Chipambano"

Njira ina yogwira mtima yokhazikitsira masomphenya autumwi m'mitima ya anthu ndiyo "mabwalo a chipambano." Mfundo imeneyi ikuchokera m'nkhani ya Davide. Asanakhale mfumu ya Israele, anatsogolera magulu ankhondo ang'onoang'ono opambana. Anthuwo analemekeza Davide ponena kuti, "Inu ndinu amene munatsogolera Aisraele pankhondo zawo (2 Sam. 5:4). Mukulankhula kwina, "Inu ndinu amene munatsogolera Aisraele kutuluka nawo

[3] Kuti mudziwe zambiri zokhudza kulimbikitsa mpingo wanu ku utumwi, onani Mutu 40: Kukhazikitsa Dongosolo la Utumwi la Mpingo Wapamalo."

ndi kubwera nao." Mawu oti "kutuluka ndi kubwera"amalankhula za kusintha kwabwino, ndipo akuwonetsera lingaliro lotsogolera ntchito zomwe zingatheke mnthawi yochepa. Kupambana kulikonse kudzalimbikitsa anthu kukhala ndi zolinga zina zoti apambane.

Mwachitsanzo, poyamba mungakonzekere kampeni ya "Pemphererani Anthu Oyandikana Nanu." Pezani mayina a iwo amene ali pafupi nanu kapena akuzungulirani ndi kulola mpingo kuwapempherera iwo. Pamene anthu ayamba kulawa chipambano, adzalimbikitsidwa kupitilira kuposa madera apafupi ndi mpingo. Zopambana zazing'ono zidzatsegula mitima yawo kuti akhale atumwi kwambiri. Adzalimbikitsidwa kuti apitilize kupitilira iwowo pazochita zomwe zikuchulukirachulukira zachipambano.

Kupambana uku kungapangitse kuwonjezereka kwa ndalama ndi maphunziro. M'kupita kwa nthawi, mpingo ukhoza kutumiza magulu a utumwi akanthawi kochepa kumatauni ndi midzi ina kuti akalalikire ndi kudzala mipingo. Ena angatengedwe kupita kumayiko ena kukathandiza atumwi kapena kudzala mipingo kumeneko. Pamene maguluwa akupereka malipoti ku mpingo, anthu alimbikitsidwa kuti achite nawo zambiri muutumwi.

GULU LA UTUMWI LA PAMALO

Kumbukirani Mwambi wakale wachiafirika wakuti, "Ngati ukufuna kufulumira, pita wekha; ngati mukufuna kupita kutali, pitani limodzi." Mudzafuna kupanga komiti ya utumwi, kapena gulu lautumwi, kuti likuthandizeni pa ntchitoyo. Abambo ndi amayi amasomphenyawa adzakuthandizani kulimbikitsa mpingo ku utumwi.

Mpingo wautumwi ungafanane ndi timu ya mpira. M'chifaniziro ichi, Mbusa sawonedwa ngati wosewera wapamwamba, koma mphunzitsi (kochi). Ndipo gulu la utumwi ndi gulu lakelophunzitsira. Mamembala a mpingo si ochemelera mu mabwalo, ndi osewera pabwalo. Ntchito ya abusa ndi gulu la utumwi ndikutenga osewera, kuwaphunzitsa, kuwalimbikitsa, ndi kuwatumiza ngati gulu lopambana.

Yesu asanasankhe ophunzira khumi ndi ndi awiriwo, anachezera usiku wonse kupemphera kwa Mulungu (Luka 6:12). Momwemonso, mudzafuna kusankha gulu la utumwi mwapemphero. Muyenera kuyang'ana anthu odzala ndi chikhulupiriro ndi Mzimu Woyera, anthu amalingaliro abwino ndi luso kuti adalitse ntchitoyo. Kenako mudzafuna kukumana ndi gulu lautumwi pafupipafupi kuti mupemphere ndi kukonzekera. Pamodzi, mudzakulitsa ulaliki wa mpingo,

kudzala mipingo, ndi madongosolo autumwi. Mudzakhazikitsa zofunika patsogolo ndikukhazikitsa bajeti ya utumwi wa mpingo.

Pamene Yesu anali pafupi kubwerera kumwamba, anasiya mpingo wake ndi lamulo lomaliza ndi lonjezo lomaliza. Lamulo lake linali lakuti, "Musachoke ku Yerusalemu, koma dikirani mphatso imene Atate wanga analonjeza, imene munandimva ine ndikunena. Pakuti Yohane anabatiza ndi madzi, koma inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera posachedwa" (Machitidwe 1:4-5). Lonjezo lake linali lakuti, "Mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu; ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero a dziko lapansi" (ndime 8).

Ndi mawu amenewa, Yesu anali kukumbutsa ophunzira ake kuti zimene zidzawachitikire posachedwapa pa Tsiku la Pentekoste n'zogwirizana kwambiri ndi nntchito yake yowombola mitundu ya anthu. Kotero, kuwonjezera, kukhala wa Chipentekoste kumatanthauza kukhala wautumwi. Izi zikutanthauza kuti munthu akhale Mbusa weniweni wa Chipentekoste ayenera kukhalamtsogoleri wachangu wautumwi. Monga mtsogoleri wautumwi, Mbusa wa Chipentekoste wasankhidwa ndi Khristu kuti atsogolere mpingo wake ku utumiki wa mphamvu ya Mzimu kunyumba kwawo ndi malekezero a dziko lapansi.

~ Gawo 8 ~

MBUSA WA CHIPENTEKOSTE MONGA OWONGOLERA

~Mutu 32 ~

Kusamalira Zolemba, Zachuma, ndi Katundu

Yesu anafotokoza nkhani ya munthu wolemera amene anapeza kuti woyang'anira katundu wake anali kuwononga katundu wake. Iye anaitana woyang'anira wosakhulupirikayo ndi kumuuza kuti afotokoze mmene anasamalirira ntchito ya bwana wake (Luka 16:1-2).

Baibulo limatiphunzitsa kuti wotsatira aliyense wa Khristu ndi woyang'anira chuma cha Mulungu. Zili choncho chifukwa chilichonse chimene ali nacho ndi cha Mulungu (Masalimo 24:1; Yakobo 1:17). Baibulo limaphunzitsanso kuti tsiku lina Mulungu adzafuna kuti Mkhristu aliyense adzafotokoze mmene iye wasamalirira chuma cha Mulungu. Paulo anachenjeza kuti, "Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Khristu, kuti yense alandire zochitika m'thupi, monga momwe anachita, kapena chabwino kapena choipa" (2 Ako. 5:10).

Mfundo yomweyi imagwiranso ntchito kwa abusa a Chipentekoste. Ayenera kukumbukira mfundo yakuti mpingo umene amatsogolera ndi wa Khristu. Amangoyang'anira mpingo wa Khristu, ndipo tsiku lina adzayankha kwa Iye momwe adasamalirira chuma chake.

MBUSA WA CHIPENTEKOSTE MONGA WOSAMALIRA

Paulo analembera Akhristu a ku Korinto kuti, “Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akhale wokhulupirika” (1 Ako. 4:2). Monga woyendetsa kapena woyang’anira woikidwa ndi Mulungu wa mpingo, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuyang’anira nyumba ya Mulungu mokhulupirika ndi mogwira mtima. Izi zikuphatikiza zonse zauzimu ndi zakuthupi za mpingo. Mbusa ayenera kuyang’anira miyoyo ya anthu mosamala. Panthawi imodzimodziyo, iye ayenera kuyang’anira mokhulupirika zina zochitika za mpingo. Izi zikuphatikizapo zolemba zapa mpingo, ndalama, ndi katundu.

Pamodzi ndi mphatso za atumwi, aneneri, aphunzitsi, zozizwa, ndi zina, Mulungu wapatsa mpingo mphatso ya “chitsogozo,” kapena, monga momwe mamasulidwe ena amamasulira, mphatso ya “kuyang’anira,” kuthandiza kumanga thupi la Khristu (1 Akorinto 12:28). Paulo analemba kuti “woyang’anira amayang’anira banja la Mulungu” (Tito 1:7). Choncho ndi udindo wa abusa kuyang’anira bwino mpingo wa Mulungu. Paulo anauza Tito kuti, mwa zina, woyang’anira ayenera kukhala “wopanda cholakwa… woongoka… ndi wodziletsa (ndime 8). Aliwonse a makhalidwe amenewa ndi makhalidwe a woyang’anira wabwino.

Ngakhale kuti nkhani za kayendetsedwe kabwino zomwe zakambidwa mu mutuwu zingathe kuwoneka za wamba kwa ena, ndi kutali ndi maitanidwe a Mbusa waChipentekoste, komabe ndi zofunika kwambiri. Mmene Mbusa amachitira ndi nkhani zimenezi zingakhudze kwambiri utumiki wake waubusa. Abusa a Chipentekoste omwe amalephera kusamalira bwino zinthu zosakhalitsa za mpingo akhoza kudzilepheretsa okha kuti asamalire zinthu zauzimu. Petro analangiza kuti, “Aliyense wa inu agwiritse ntchito mphatso iliyonse imene walandira potumikira ena, monga adindo okhulupirika a chisomo cha Mulungu cha mitundu-mitundu” (1 Petro 4:10).

Ngakhale kuti mpingo ndi woposa ntchito, komabe ndi ntchito. Kumlingo wauukulu, chipambano cha ntchito iliyonse chimadalira mmene imalinganizidwira bwino ndi kusamaliridwa. Ena amanena kuti popeza kuti mpingo ndi chinthu chamoyo osati bungwe, ndiye kuti sikufunika dongosolo la bungwe. Mawu awa ndi oona mwatheka. Ndi zoona kuti mpingo, monga thupi la Khristu, ndi chinthu chamoyo. Komabe, sizowona kuti sikufunika dongosolo. Kunena zoona, chamoyo chilichonse mwachibadwa n’nchadongosolo kwambiri.

Machitsanzo, m'thupi la munthu, mutu uli ndi malo ake, monganso thunthu, mikono, miyendo, ndi zina zotero.

Bungwe limalankhula za dongosolo, ndipo zimaonetsera kuyesayesa kogwirizana. Mipando yodzaza galimoto ingakhale yamtengo wapatali, koma imakhala yosathandiza kwenikwenikufikira itatsitsidwa m'galimotoyo n'kuikidwa m'nyumbamwadongosolo. Mofananamo, kuti mpingo ufike pamlingo waukulu, uyenera kulinganizidwa bwino.

Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kuyesetsa kukulitsa luso lake la utsogoleri. Ndipo mpingo uliwonse uyenera kukhala ndi njira zogwirira ntchito zoyendetsera ntchito yake. Pamene mpingo ukutakasuka ndikukula, dongosolo lake la kayendetsedwe kake lidzakhala lovuta kwambiri komanso machitidwe ake osunga zolemba bwino. Maudindo atatu oyang'anira a Mbusa aliyense wa Chipentekoste ndi (1) kusunga zolemba za mpingo, (2) kuyang'anira ndalama za mpingo, ndi (3) kusamalira katundu wa mpingo. Mbali yotsala ya mutuwu ifotokoza za udindo wa abusa.

KUSUNGA ZOLEMBA ZA MPINGO

Mbusa wa Chipentekoste wamphamvu adzagwiritsa ntchito nthawi ndi mphamvu zofunikira kuti asunge zolemba za mpingo zolondola komanso zamakono. Zolemba izi zidzapindulitsa abusa ndi mpingo munjira zinayi zofunika:

Choyamba, dongosolo losunga zolembedwa lolinganizidwa bwino lidzatheketsa kuti Mbusa apeze chidziwitso chofunika pamene chifunika. Ndipo chifukwa zolembazo zimasungidwa bwino,kaundula adzakhala wodalirika.

Chachiwiri, zolemba zosungidwa bwino zingathandize abusa kusamalira ndi kuteteza katundu wa mpingo. Iwo akhoza kukhala umboni walamulo la mpingo ndi zochita zachuma. Mwachitsanzo, ngati wina akutsutsa umwini wa malo a mpingo wa pamalo, Mbusa adzatha kutulutsa chikalatacho ndi kutsimikizira zoona zake.

Chachitatu, zolemba zabwino zimapatsa Mbusa wa Chipentekoste chidziwitso chomwe akufunikira kuti apange zisankho zanzeru za tsogolo la mpingo. Mwachitsanzo, poona kuchuluka kwa opezekapo zaka zapitazo, abusa akhoza kusonyeza kukula kwa mpingo m'tsogolo. Izi zitha kuthandiza atsogoleri kupanga zisankho pa zantchito zamtsogolo ndi zosowa za ogwira ntchito. Mofananamo, pofufuza maukwati angati amene anali kukondwelera zaka za

m'mbuyomo, Mbusa angayelekeze maukwati angati amene adzachitika m'chaka chimenechi. Athanso kugwiritsa ntchito zomwe zidachitika kale kulosera zam'tsogolo.

Chachinayi, zolemba zabwino zimapatsa abusa ndi mpingo kulumikizana ndi zakale. Zimathandiza kudziwitsa abusa ndi mamembala zomwe zidawatsogolera. Cholembedwa cha m'mbiri chimenechi chidzathandiza kuyamikira amene munatenga malo awo ndipo chidzawapatsa lingaliro la kukhala nawo ndi kukhala mosadzasintha.

Mfundo Zoyendetsera Zolemba Zabwino

Nthawi idzafika pamene Mbusa aliyense adzafunsidwa kuti apereke utsogoleri kwa wolowa m'malo. Mbusa wokhulupirika wa Chipentekoste adzakonzekeretsa mpingo ku chochitika chosapeweka chimenechi. Njira imodzi imene angachitire zimenezi ndi kusunga zolemba za mpingo zolondola. Nazi mfundo zisanu zosunga bwino mbiri:

1. *Zolondola.* Zolemba zonse ndi zikalata ziyenera kukhala zolondola. Zikuyenera kuyimira mbiri yeniyeni ya zomwe zachitika.
2. *Zolinganiza.* Zolemba za mpingo ziyenera kukonzedwa bwino. Ziyenera kukonzedwa m'magulu omveka bwino, motero zimapereka mwayi wopeza chidziwitso pakafunika.
3. *Pa nthawi yake.* Zolemba ziyenera kusungidwa mwamakono. Zochita zonse zachuma ziyenera kutumizidwa mwamsanga. Zochita zina, monga mdalitso wa ana, ubatizo, ndi maukwati, ziyenera kulembedwa panthawi yake.
4. *Zomalizitsa.* Zolemba za mpingo ziyenera kukhala zonse. Mfundo zonse zokhudzana ndi chochitika kapena kugula ndi kugulitsa ziyenera kulembedwa.
5. *Zotetezeka.* Zolemba zonse ziyenera kusungidwa pamalo otetezeka, otetezedwa kwa kuba ndi nyengo yoipa.

Zolemba Zolondola

Mbusa wa Chipentekoste awonetsetse kuti zolemba zolondola za misonkhano yonse ya mpingo zikusungidwa. Izi zikuphatikizapo misonkhano ya mwezi ndi mwezi ya komiti yaikulu yapa mpingo, misonkhano yapachaka yopereka kumpingo onse mmene utumiki wayendera, ndi misonkhano yapadera yodziwitsa mpingo mmene ntchito ya utumiki ikuyendera. Zolemba za msonkhano uliwonse

ziyenera kusungidwa ndi mlembi woikidwa ndi kudzipereka pamsonkhano wotsatira kuti zivomerezedwe. Zikavomerezedwa, ziyenera kusainidwa ndi mlembi ndi Mbusa n'kuikidwa m'mabuku akaundula wazochitika pa mpingo kuti adzawagwiritse ntchito m'tsogolo.

Kaundula wa Zochitika

Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kusunga kaundula wa zochitika zatsopano. Kaundulayu aphatikiza zolembedwa za mamembala ampingo, ubatizo wa mmadzi, maukwati, kudalitsidwa kwa ana, ndi mabweredwe a ku mpingo motere:

Umembala wa mpingo. Kaundula wa zochitika za mpingo ayenera kukhala ndi mnndandanda wa mamembala a mpingo. Mayina onse a mamembala atsopano ayenera kuwonjezeredwa pamndandanda akalandiridwa ngati mamembala. Mndandandawo uyeneranso kukhala ndi tsiku lomwe adalandiridwa ndi ndemanga zina zokhudza kulandiridwa kwawo. Pamene membala aliyense amwalira kapena kusiya mpingo, zochitika zimenezi ziyenera kuzindikiridwa. Ndi bwino kupereka satifiketi ya umembala kapena khadi kwa mamembala atsopano ngati gawo lamwambo wowalandira. Zobwereza ziyenera kusungidwa m'mafaelo ampingo.

Ubatizo wa Madzi. Kaundula wa zochitika ayeneranso kukhala ndi mndandanda wa amene anabatizidwa m'madzi. Payenera kuonetsanso tsiku la ubatizo ndi zaka zawo pamene anabatizidwa. Satifiketi ya ubatizo iyenera kuperekedwa kwa aliyense amenewabatizidwa.

Maukwati. Kaundula wa zochitika za mpingo ayenera kukhala ndi mbiri ya onse okwatirana mu mpingo. Cholembedwachi chiyenera kukhala ndi tsiku laukwati ndi mayina onse a mkwati ndi mkwatibwi. Iyeneranso kuphatikiza dzina la mtumiki (kapena atumiki) otsogolera mwambowu, komanso mndandanda wa onse omwe adachita nawo mwambowu. Abusa angafunenso kulemba tsiku limene okwatiranawo analengeza mwalamulo za chinkhoswe chawo ku mpingo. Pambuyo pa mwambo waukwati, kalata yaukwati iyenera kuperekedwa kwa okwatiranawo. Abusa akuyenera kutsatira malamulo onse okhudza ukwati.

Mdalitso wa Ana. Mbusa wa Chipentekoste alembenso chiwerengero cha mwambo wamdalitso wa ana omwe wachitika pa mpingo. Mipingo ya Chipentekoste sibatiza makanda, iwo amachita mdalitso wa ana. Kupereka kwa Hana kwa mwana wake, Samuele, kumapereka chitsanzo chabwino cha mchitidwe

umenewu (1 Samuele 1:21-28). Pambuyo pa mwambo wa mdalitso, Mbusa ayenera kulemba dzina lonse la mwanayo m'kaundula wa zochitika, pamodzi ndi tsiku la kubadwa kwa mwanayo, kumene mwanayo anabadwira, ndi tsiku la mwambowo. Pamndandanda umeneu palinso mayina a bambo ndi mayi, keyala ya makolo awo ndi manambala awo a foni, ndi zina zofunika kuziona. Mbusa apereke chikalata cha mdalitso kwa makolo.

Mabweredwe Kumpingo. Mbusa ayeneranso kuonetsetsachiwerengero chammene anthu akubwerera kumpingo mlungu uliwonse. Cholembedwa ichi chiyenera kuphatikizapo tsiku ndi chiwerengero cha anthu amene amabwera m'kalasi lililonse la Maphunziro a Baibulo (Sande Sukulu), kulambira kwa Lamulungu m'mawa, utumiki wa Lamulungu madzulo, kuphatikizapo ndi misonkhano ya ana, achinyamata, ndi yapakati pa sabata. Zolemba izi ziyenera kusungidwa ndi Mbusa kapena mlembi wa mpingo.

Kaundula wa Ulaliki

Kuwonjezera pa kaundula wa mpingo, mudzafuna kusunga mbiri yanu ya maulaliki amene mumalalikira. Nthawi iliyonse mukakamba ulaliki, kuphunzitsa phunziro, kapena kulankhula pagulu la anthu lililonse, mudzafuna kujambula zomwe zachitika mu kaundula wa ulaliki. Chilichonse cholembedwa mukaundulayu chiyenera kukhala ndi tsiku, chochitika, ndi malo amene uthengawo unaperekedwa. Chiyeneranso kukhala ndi Malemba ogwiritsidwa ntchito, limodzi ndi mutu wa uthengawo. Mungafunanso kutchulapo Mfundo zofunika, monga mmene anthu amayankhira uthengawo. Kaundulayu akuthandizani kuti muzisunga mauthenga anu, komanso kuti muunikenso ndondomeko yanu yolalikira. Mudzafunanso kusunga zolemba zanu zaulaliki pamalo otetezeka kuti mudzazigwiritse ntchito m'tsogolo.

KUYANG'ANIRA NDALAMA ZA MPINGO

Mbusa wa Chipentekoste awonetsetsenso kuti zolembedwa zolondola komanso zanthawi yake zikusungidwa pazochitika zonse zachuma zokhudzana ndi mpingo. Mchitidwewu udzaonetsetsa kuti ndalama za mpingo ziziyendetsedwa bwino nthawi zonse. Zithandizanso kuteteza abusa ndi atsogoleri a mpingo ku milandu yosokoneza ndalama za mpingo.

Kulandira ndi Kusamalira Zopereka

Mipingo yambiri ya Chipentekoste mu Afirika imalandira ndalama makamaka kudzera mu chakhumi ndi zopereka zomwe zimalandiridwa pa mapemphero awo a Lamulungu m'mawa. Ngakhale kuti zoperekazi zikhoza kulandiridwa motsatira miyambo ya mpingo, Mbusa ayenera kuonetsetsa kuti zopereka zonse zikuchitidwa moona mtima komanso mosabisa.

Kuti achite izi, ayenera kuwonetsetsa kuti zopereka zikulandiridwa ndikuwerengedwa ndi akuluakulu odalirika awiri kapena kuposerapo. Akamaliza kuwerenga choperekacho, akuluakulu omwewo ayenera kulemba fomu yoperekera. Pa fomu yoperekerayo payenera kukhala malo olemba tsiku, mtundu (kapena mitundu) wa zopereka zolandiridwa, ndi mayina ndi masiginecha a amene akuwerenga ndalamazo. Fomu yoperekera iyeneranso kukhala ndi mizere yolembera mtundu uliwonse wa zopereka zomwe zalandiridwa. Mwachitsanzo, mzere umodzi ulembedwe "chakhumi," wina ulembedwe "zopereka zaufulu," wina "ndalama zachitukuko," ndi zina zotero. Owerengerawo awonetsetse kutikuchuluka kwa chopereka chilichonse chomwe chalandiridwachikuyikidwa m'gulu lake loyenera.

Mafomu azoperekawa ayenera kupangidwa mosinikiza zingapo, ndipo pepala limodzi lipite kwa msungichuma wa mpingo ndipo linalo lipite kwa abusa. Msungichumayo adzawerengeranso ndalamazo ndikulowetsa ndalama zonse zomwe zalandiridwa m'kaundula wa mpingo m'gulu lake loyenerera. Kenako adzaika ndalamazo kubanki. (Ngati n'kotheka, mpingo uliwonse ukhale ndi akaunti yakubanki. Ngati izi sizingatheke, ndalamazo ziyenera kusungidwa mu malo otetezeka kapena okhoma bwino.) Msungichuma ayenera kusunga lisiti ya kusungitsa ndalama ku banki ngati mbiri ya mpingo.

Kusunga Zolemba Zachuma

Zolemba zowerengera zitha kusungidwa pa pepala kapena pa kompyuta. Ngati kompyuta ikugwiritsidwa ntchito, kungakhale kwanzeru kupanga malipoti a mapepala sabata lililonse kuti muwaike m'faelo, popeza kuti nthawi zina makompyuta amawonongeka. Nthawi iliyonse ndalama zikulandiridwa kapena kuperekedwa, zomwe zikuchitikazo zilembedwa pa lisiti ya ndalama. Lisiti limeneli limaperekedwa kwa msungichuma wa mpingo amene amalemba mndondomeko yosungiramo mbiri ya ndalama.

Mbusa aliyense wa Chipentekoste ayenera kuphunzira kuwerenga ndi kusanthula buku la ndalama. Luso limenelilidzathandiza kuti aziona mmene ndalama za mpingo zimagwirira ntchito komanso kudziwa kuchuluka kwa ndalama zimene zimapezeka m'thumba lililonse panthawi iliyonse. Mchitidwewu udzathandiza abusa ndi atsogoleri a mpingo kupanga zisankho zanzeru zachuma. Ndipo zidzathandiza kuonetsetsa kuti zolemba zachuma za mpingo zikusamalidwa bwino.

Kupereka Ndalama za Mpingo

Chopereka chilichonse choperekedwa ku mpingo chiyenera kugwiritsidwa ntchito pa cholinga chimene chaperekeredwa. Mwachitsanzo, n'kosaloleka kutenga ndalama zoperekedwa ku thumba la zomangamanga n'kuzigwiritsa ntchito pogulira abusa galimoto. Nthawi zonse ndalama zikaperekedwa kapena kusamutsidwa kuchokera kwa munthu m'modzi kapena pologalamu kupita ina, iyenera iperekeredwe lisiti, ndipo lisitiyo iyenerakuperekedwa kwa msungichuma kuti awerengere bwino. Malisiti onse ayenera kusungidwa m'mafaelo owerengera ndalama a mpingo.

Malipoti Azachuma

Kumapeto kwa mwezi uliwonse, msungichuma wa mpingo ayenera kukonza lipoti la ndalama kwa abusa ndi komiti yaikulu. Lipotili lipatsa utsogoleri wa mpingo mbiri yolondola ya ndalama ndi ndalama zomwe zagwiritsidwa ntchito mwezi wathawu. Izi zidzawathandiza kupanga zisankho zanzeru pa nkhani ya ndalama za mpingo. Kuphatikiza pamalipoti azachuma a mwezi uliwonse, msungichuma wa mpingo ayenera kutulutsa lipoti la zachuma lapa chaka ndikulipereka kwa abusa ndi komiti yaikulu yapa mpingo. Zotsatira zake Abusa ndi komiti yaikulu nawonso adzipereka lipoti la zachuma la pachaka kwa ku mpingo pa msonkhano wapachaka wokambirana momwe ntchito ya utumiki inayendera pampingo.

Ndondomeko ya chuma (Bajeti)

Ndikofunika kuti Mbusa wa Chipentekoste adziwe kukonzekera ndi kutsatira ndondomeko ya bajeti ya mpingo. Mchitidwewu udzawathandiza kuti azisamalira bwino ndalama za mpingo. Bajeti ndi dongosolo lazachuma. Ndi kuyerekeza ndalama zomwe mpingo umalandira m'chaka chomwe chikubwerachi komanso ndondomeko yogawa ndalamazo. Bajeti yabwino idzaonetsa cholinga cha mpingo

ndi zofunikira zake. Mwachitsanzo, ngati mpingo uika patsogolo utumwi ndi kudzala mipingo, bajetiyo iyenera kuwonetsa izi. Mwanjira imeneyi, bajetiyo imatha kuwonedwa ngati chikalatachautumwi.

Kukonzekera bajeti ya mpingo kumafunika kuti Mbusa ndi a komiti yaikulu ayang'ane mmene mpingo wachitira pa nkhani zachuma m'zaka zam'mbuyomo. Kenako, pogwiritsa ntchito chidziwitsocho, angapange zisankho zanzeru za mmene mpingo udzagawira ndalama zake m'chaka chimene chikudzacho. Mchitidwe umenewu udzathandiza kuwonetsetsa kuti ndalama za mpingo zisawonongeke pazinthu zazing'ono, pamene zinthu zofunika kwambiri zikusiyidwa osadzipatsa ndalama.

Bajetiyi ili ndi magawo awiri akulu: ndalama zomwe zikuyembekezeka komanso ndalama zomwe zidzagwire ntchito chaka chamawa. Ndalama zoyembekezeka ziphatikiza chakhumi, zopereka, ndi zina. Ndalama zomwe zidzagwire ntchitozidzaphatikizapo ndalama zokhazikika (monga malipiro, ngongole zanyumba, ndi zofunikira monga magetsi/madzi) ndi ndalamazogwira ntchito zina zosiyanasiyana (monga zinthu zaofesi, zipangizo za Maphunziro a Baibulo, kudzindikiritsa kwa ena zochitika pampingo, ndi kukonza nyumba). Mpingo uyeneranso kupanga bajeti ya ndalama ya zinthu zosayembekezereka komanso zadzidzidzi. Poyamba, kupanga bajeti kumakhala kovuta. Komabe, pambuyo pa zaka ziwiri kapena zitatu za kufufuza mokhulupirika ndalama zolowa ndi zotuluka za mpingo, ndondomeko ya bajeti idzakhala yosavuta. Zidzakhala zothandiza kwambiri pakugwira ntchito ku mpingo.

KUSAMALIRA KATUNDU WA MPINGO

Monga mdindo wa katundu wa Mulungu, Mbusa wa Chipentekoste ayenera kuonetsetsa kuti chuma cha mpingo chikusamalidwa bwino. Zinthuzi zikuphatikizapo zolemba zofunika zapa mpingo komanso nyumba yopempheleramo, malo, ndi zina.

Kusunga Zolemba Zamalamulo

Mbusa ayenera kuonetsetsa kuti zikalata zamalamulo za mpingo zikusungidwa mwadongosolo komanso kusungidwa pamalo otetezeka. Ngati n'kotheka, zikalata zimenezi ziyenera kusungidwa pamalo abwino kapena m'kabosi kosungiramo kotetezeka ku banki. Ndondomeko yolongosola katundu

amene ali kumalo otetezekawa ilembedwe ndikusungidwa m'mafaelo aku mpingo.

Kusamalira Katundu wa Mpingo

Mbusa wa Chipentekoste alinso ndi udindo wowona kuti nyumba ya tchalitchi ndi mabwalo akusamalidwa bwino. Angafune kusankha komiti yoyang'anira udindo umenewu. Komiti imeneyi idzaonetsetsa kuti katundu wa mpingo asamaliridwe monga momwe zingakhalire ndi nyumba ya Mulungu. Pansi ndi ndi malo ayenera kusesedwa ndikusungidwa opanda zinyalala. Mipanda iyenera kupakidwa utoto ndi kuitsuka bwino lomwe. Mazenera ayenerakukhala aukhondo komanso abwino. Ndalama zopangira zomanga ndi kukonza malo ziyenera kukhala mbali ya ndalama zomwe mpingoyu udaika kuti zigwire ntchito imeneyi.

Zomwezo zimapitanso ku ziwiya ndi zipangizo zonse za mpingo. Zipangizo zimenezi ndi monga guwa/gome, mipando, mipando ya muofesi, ndi zokuzira mawu ziyenera kukhala zaukhondo ndi zokonzedwa bwino. Pakafunika kukonza, ziyenera kuchitidwa munthawi yake.

~ Mutu 33 ~

Kusonkhanitsa Atsogoleri Omwe si Abusa

Ku Afirika, ndi chosadabwitsa kuwona ana akusewera mpira wa miyendo pa bwalo. Ena amasewera mpira weni-weni, opopa. Pomwe ena makamaka akumidzi amasewera mipira yopanga okha, nthawi zina yopangidwa ndi zipepala za pulastiki zokulunga ndi kumanga ndi zingwe. Ndizopatsa chimwemwe chachikulu kuwawona akuthamanga, kuseka ndi kudzipereka kusewerera m'matimu awo.

Ena mwa anawa amachita mwayi osewera nawo mutimu yoyimira dera lawo. Kumeneko, amaphunzirako kufunika kogwira ntchito limodzi ngati gulu komanso kusewera kwabwino. Ma membala a timu amaphunzira kuti osewera aliyense ndi ofunikira komanso waphindu ku timu yonse. Kuti timu ichite bwino, osewera aliyense amayenera kudzipereka kwathunthu. Angakhale kuti timu ikugonja, osewera aliyense amalimbikirabe, ndikumalimbikitsana wina ndi nzake. Anawa amaphunzira kuti timu ichite bwino kumbali yayikulu zimatengera m'mene osewerawo akudziwonera. Izi ndi kuphatikizapo onse amene ali m'bwalo kusewera komanso amene sanalowe nawo m'bwalo. Mpingo ungathe kuphunzirapo zambirikuchokera ku ma timu ampira wa miyendo omwe amayendetsedwa bwino.

Wina adafotokozera masewera a akatswiri ampira monga anthu makumi awiri ndimphambu ziwiri omwe aliwefuwefu kulakalaka atapuma koma owoneleredwa ndi anthu zikwi khumi amene akusowekera masewero olimbitsa thupi. Zachisoni, chithunzithunzi ichi chikufotokozera m'mene mipingo yambiri ya Chipentekoste ilili mu Afirika lero lino. Pamene mamembala ena ochepa amalemedwa kunyamula katundu wa utumiki, ambiri mu mpingo amathandizirapo mochepa chabe. Mipingo imeneyi yasanduka *masewera owonelera* kumene osewera ochepa chabe akuchemereredwa ndi owonerera ambiri. M'chitidwe osathandiza komanso osagwirizana ndi Baibulo ukulepheretsa mpingo kukwaniritsa ntchito ya Mulungu. Ngati mpingo ungachite bwino abusa akuyenera kuphunzira kumemeza ma membala kuti atengepo gawo pa kutumikira ufumu wa Mulungu.

Mutuwu uonetsera vutoli. Choyamba, uika maziko a Baibulo pa utsogoleri wa omwe si abusa mu mpingo. Kenako upereka malangizo ochitika a mmene inu, ngati Mbusa wa Chipentekosite, muntha kusokhanitsira anthu wamba ku utumiki mu mpingo komanso dera lanu.

CHOMWE BAIBULO LIMANENA

Kuyambira pa chiyambi cha Mpingo, atumwi anaona kufunikira komemeza aliyense ku utumiki opatsidwa mphamvu ndi Mzimu. Komanso, kodi Yesu sanalonjeza kuti, "komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko" (Machitidwe 1:8). Lonjezano ili silinali kwa atumwi okha. Linali la kwa Mkhristu wina aliyense, Mbusa komanso membala chimodzimodzi. Dongosolo la Yesu pa Mpingo linali lakuti membala wina aliyense adzazidwe ndi Mzimu ndi kuti aliyense atengepo mbali pokwaniritsa ntchito yayikulu ya Mulungu yofalitsa Uthenga Wabwino kudziko lonse la pansi.

Mpingo Oyamba

Posakhalitsa Mzimu atangotsanulidwa pa Tsiku la Pentekoste, mpingo oyamba unayamba kukonza machitachita olalikira ndi kukonza maphunziro a okhulupirira. Baibulo linena kuti, "Ndipo anali chikhalire m'chiphunzitso cha atumwi ndi m'chiyanjano" (Mach. 2:42). Ndipo liwonjeza kuti, "Ndipo tsiku ndi tsiku anali chikhalire ndi mtima umodzi mu Kachisi… nalemekeza Mulungu, ndi kukhala nacho chisomo ndi anthu onse. Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe" (vv. 46-47). Atsogoleri anafunikira kuti

asamalire magulu otumphuka mwakathithi a anthu omwe amasonkhana mnyumba. Atumwimosakaikira anayamba kuphunzitsa ena mwa otembenuka mtima kumenewa maphunziro a utsogoleri ndi utumiki.

Pamene mpingo umakula ndi kuchita bwino, ena anayamba kukhala nawo mugulu la atsogoleri. Amuna ndi amayi amenewa amatumikira pansi pa atumwi ndikuthandizira pa ntchito yawo. Lero timawatcha anthu amenewa atumiki (Dikoni). Atumwi anakhazikitsa kuti atsogoleri osakhazikitsidwawa akhale odzala ndi Mzimu ndi nzeru. Ntchito yawo inali ku yendetsa dongosolo la zakudya ku akazi amasiye a Chihelene amena anatembenuka mtima (Machitidwe 6:1-7). Nzosakayikitsa kuti udindo wa anthu amenewa unasintha pamene zosowa zina zinatumphuka. Awiri a iwo, Stephano ndi Fillipo, anasanduka alaliki amphamvu a uthenga wa bwino.

Patatha zaka, dongosolo la mpingo litakhazikika, Paulo analongosolera mpingo wa ku Aefeso ndondomeko ya utsogoleri wa mpingo. Mpingo umayenera kutsogoleredwa ndi Atumwi, aneneri, alaliki, abusa, ndi aphunzitsi (Aefeso 4:11). Komabe atumikiamenewa samayenera kutumikira paokha. Ntchito yawo ndi "kukonzekeretsa anthu a Mulungu kuntchito ya utumiki" (v. 12). Amayenera kudzutsa atsogoleri pakati pa otembenuka mtima kuti awathandizire pa nchitoyi. Ngati akanachita ichi, mpingo ukadakhala wamphamvu ndi ochitachita (vv. 11-16).

Unsembe ndi Uneneri wa Okhulupirira Onse

Baibulo limaphunzitsa za "Unsembe wa Okhulupirira onse." Izi zikutanthauza kuti otsatira Khristu aliyense ndi wa nsembe pamaso pa Mulungu. Monga wa nsembe, iye ali ndi mphamvu zowerenga komanso kutanthauzira malemba ndi kugawana chisomo cha Mulungu ndi ena (1 Petro. 2:5, 9). Baibulo limapitilira kuphunzitsanso za "uneneri wa okhulupirira onse." Izi zikutanthawuza kuti pakungobadwa kwa tsopano ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, okhulupirira aliyense wasanduka gawo la khamu la Mulungu la uneneri la m'masiku otsiliza (Numeri. 11:29; Yowele 2:28-29; Machitidwe 2:17-18). Pakuwapatsa Mzimu Wake, Mulungu wawapatsa mphamvu kukhala mboni za Khristu "Mu Yerusalemu, ndi mu Yudea ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake adziko" (Machitidwe 1:8).

Pa Tsiku la Pentekoste, Petro anayamba uthenga wake polengeza "komatu ichi ndi chimene chinanenedwa ndi mneneri Yowele, Ndipo kudzali m'masiku

otsiriza, anena Mulungu, Ndidzathira cha Mzimu wanga pa thupi lililonse, ndipo ana anu aamuna, ndi aakazi adzanenera, ndipo anyamata anu adzaona masomphenya, ndi akulu anu adzalota maloto" (Machitidwe 2:16-17). Petro anatsiliza uthenga wake polamulira anthu, "komatu ichi ndi chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoeli, Ndipo kudzali m'masiku otsiriza, anena Mulungu, Ndidzathira cha Mzimu wanga pa thupi liri lonse, Ndipo ana anu amuna, ndi akazi adzanenera, Ndipo anyamata anu adzaona masomphenya, ndi akulu anu adzalota maloto; Koma Petro anati kwa iwo, "Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezano lili kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzaitana" (vv. 38-39). Petro ankanena kuti tsiku lafika pamene anthu a Mulungu adzamtumikire Iye monga atumiki opatsidwa mphamvu ndi Mzimu.

Kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera kumayenereza anthu onse, posatengera kuti ndi onyozeka kapena osalidwa motani, kuti ayankhule ndi ku tumikira Khristu. Mbusa wa Chipentekoste akuyenera kuzindikira chinthu ichi ndipo ayenera kulimbikitsa anthu ake kuti adzazidwe ndi Mzimu Woyera kuti akhale ochitachita pa utumiki wapa mpingo.

KUSOWEKERA KWA ATSOGOLERI OMWE SI ABUSA

Kuti Mpingo uphukire ndi kukukula monga m'mene Mulungu afunira, ukuyenera kukhala ndi utsogoleri wa mphamvu wa abusa. Ukuyeneranso kukhala ndi utsogoleri wa mphamvu wa iwo amene si abusa.

Chovuta chachikulu chimene mipingo yambiri ya Chipentekoste ikukumana nacho lero ndi chakuti mamembala ake ochuluka ndiosaphunzitsidwa mokwanira. Ichi chafooketsa mpingo kwakukulu. Chifukwa choti anthu sanaphunzitsidwe, azibusa akumagwiranso ntchito zimene anayenera kumachita okhulupirira ena pa mpingo. Zotsatira zake, azibusa amatanganidwa kwambiri ndi ntchito zina zing'ono zing'ono zimene alibe nazo mpata komanso changu kuti azichite molongosoka.

Nkhani ya Yetero ndi Mose ikuwonetsera Mfundo imeneyi (Eksodo. 18:13-26). Mose anatsogolera a Israele kutuluka muukapolo wa Aejipito. Tsopano analikubwera kwa iye kuti awaweruzile milandu yawo ndi kuwayanjanitsa. Kumabwera anthu ochuluka kotero kuti Mose amati akayamba kuweruza milandu

yawo, amakhala kuyambira m'mamawa mpakana madzulo. Izi zimapitilira tsiku ndi tsiku. Popita nthawi, Mose anafika polema.

Pamene Yetero, mpongozi wake wa Mose anawona zimene zimachitika, anamulangiza Mose "chinthu uchitachi sichili chabwino ai…..pakuti chikukanika chinthu ichi; sungathe kuchichita pa wekha." (vv. 17-18). Yetero anamuuza Mose, "Koma iwe, dzisankhire mwa anthu ako onse… nuwaikire iwo oterewa… ndipo iwo aweruze milandu ya anthu nthawi zonse; ndipo kudzakhala kuti milandu yaikulu yonse abwere nayo kwa iwe… potero idzakuchepera nchito, ndi iwo adzasenza nawe" (vv. 21-22). Mose anatsatira malangizo a Yetero. Zotsatira zake anthu anatumikiridwa bwino ndipo Mose anapeza mpumulo.

Monga Mbusa wa nzeru wa Chipentekoste, ukuyenera kuchita chimodzimodzi. Ukuyenera kusankha amuna ndi akazi oopa Mulungu kuti akuthandizire ntchito. Uyenera kuwaphunzitsa ndikuwakhazikitsa kuti adzigwira ntchito zawo. Ngati ungachite izi, udzamasuka ku ntchito ya mpingo ya tsiku ndi tsiku. Ndipo udzakwanitsa kukhazikika pa ntchito zimene iwe wekha ndamene ungakwanitse kuzigwira. Mapeto ake, mpingo wako udzachita bwino.

Kusintha kwa Chindunji

Kuti uchite izi, pukuyenera kusintha chindunji. Uchoke podziona wekha ngati katswiri mu timu ndi kuyamba kudziona ngati ndiwe mphunzitsi wa osewera. Ntchito yako sindiyo yogoletsa zigolikomano kuphunzitsa anthu m'mene angagoletsele zigoli. Ntchito yako sindiyo kupereka uphungu kwa anthu onse, koma kuonetsetsa kuti anthu onse alandira uphungu wa nzeru (Eksodo 18:21-22). Ntchito yako sikudyetsa amayi onse amasiye a Chihelene, koma kuonetsetsa kuti amayi amasiye a Chihelenewa akupatsidwa chakudya moyenera (Mach. 6:1-3). Mwanjira ina, monga Mbusa, ntchito yako ndiyo "kukonzekeretsa anthu a Mulungu kuntchito ya utumiki" (Aef. 4:11-12). Kuchokera pa chiyambi pomwe pa utumiki wako, ukuyenera ku konzekeretsa ma membala ku utumiki. Gulu la atsogoleri pakati pa anthu litumphuka pakati pa iwo amene akuphunzitsidwa.

Kusonkhanitsa Atsogoleri Omwe si Abusa

Monga Mbusa, ukuyenera kuzindikira, kuphunzitsa, ndi kumasula atsogoleri pakati pa ma membala. Udziwona ma membala a mpingo wako ngati timu yomwe ili ndi anthu a mphatso ndi upangili omwe ukhoza kusonkhanitsidwa kuti utumikire mu ufumu wa Mulungu. Kuti timu ichite bwino, osewera aliyense

akuyenera kuchita mbali yake. Mtsogoleri yemwe si Mbusa ndi wina aliyense amene watenga udindo wa utsogoleri wa utumiki wina mumpingo. Zitsanzo ndi monga, ma dikoni (atumiki), akulu ampingo, oyang'anira komanso ophunzitsa maphunziro a Sukulu ya Baibulo lamulungu, atsogoleri a ku mlaga, atsogoleri a amayi ndi abambo, atsogoleri a aChinyamata, otsogolera utumiki wa ana, otsogolera kwaya, atsogoleri a gulu la malambiro, atsogoleri a utumwi ndi ena otere.

ZOYENEREZA ATSOGOLERI OMWE SI ABUSA

Chingakhale kuti Membala wina aliyense wa mu mpingo anayitanidwa kuti atumikire, si onse omwe adziyenereza okha. Kutumikira monga mtsogoleri mu mpingo, munthu ayenera kudziyika yekha pa mulingo omwe unakhazikitsidwa m'mawu a Mulungu. Paulo anati za atumiki (ma dikoni), "Koma iwonso ayamba ayesedwe; pamenepo atumikire, akakhala opanda chifukwa" (1 Timoteo 3:10).

Atumwi ku Machitidwe adakhazikitsa zoyenereza za maziko ziwiri: "Odzala ndi Mzimu ndi nzeru" (Mach. 6:3). Mu 1 Timoteo 3 and Tito 1, Paulo analongosola tsatanetsatane wa zoyenereza atsogoleri a mpingo. Pamene zambiri mwa zoyenerezazi ndizokhudza abusa ndi akulu a mpingo, ndi zofunikirabe poganizra za zoyenereza udindo wa utsogoleri wina uliwonse mu mpingo.

Kochokera mundandanda umenewu tingathe kupezapo zigawo zisanu zoyenera kuziganizira posankha atsogoleri a mpingo. Zigawo zimenezi ndi (1) khalidwe lovomerezeka la mtsogoleri, (2) moyo wawo wa uzimu, (3) chikhalidwe chakudekha, (4) Khalidwe lawo la tsiku ndi tsiku, ndi (5) umboni wawo mdera lomwe akukhala. Abusa asankhe anthu okhawo m'ma udindo amene ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera, opembedza, odzipereka, ophunzitsika komanso ololera kutumikira pansi pa Mbusa monga otsogolera anzawo.

KUSANKHA NDI KUPHUNZITSA ATSOGOLERI OMWE SI ABUSA

Monga momwe mphunzitsi angafufuzire osewera akazi ndi amuna odziwa bwino kusewera kuti asewere mu timu yake, nawenso monga mtsogoleri osankhidwa ndi Mulungu, uyenera kufufuza anthu oyenelera kuti atsogolele ma utumiki apa mpingo. Pamene palibe atsogoleri oyenerezeka, uyenera kuwaphunzitsa. Yesu anachita chimodzimodzi ndi akuphunzira ake, ndipo Paulo anatero ndi Timoteo komanso Tito, ndi ena. Tiyeni tiwone magawo awiri

amenewa osonkhanitsa atsogoleri omwe si abusa mu mpingo: Kusankha ndi kuphunzitsa kapena kuumba atsogoleri.

Kusankha Antchito

Ntchito yosankha atsogoleri omwe si abusa imafunika kukambirana mofatsa ndi iwo amene ali kale atsogoleri pa mpingo. Imafunikanso mapemphero ochuluka, kufunafuna Mulungu kuti atsogolere. Izi ndi zimene Yesu anachita. Munthawi yonse ya utumiki wake, anapitilirabe kusaka chitsogozo cha Atate wake (Luka 5:16). Mwachitsanzo, asanasankhe ophunzira ake khumi ndi awiri, Yesu "ananka kuphiri kukapemphera; nachezera usiku wonse m'kupemphera kwa Mulungu" (6:12).

Pamene walandira chitsogozo kuchokera kwa Ambuye, ukuyenera kukonzeratu kuti ndi antchito anji adzafunike kuti ntchito ikwaniritsidwe. Kenakano ugawane nawo masomphenya mpingo ndikufunsa amene angadzipereke. Pofunsa amene angadzipereke, ndi zofunikira kulonjeza kuti maphunziro antchitoyo adzaperekedwa kwa odzipereka. Izi zidzalimbikitsa anthu ochuluka kudzipereka. Atsogoleri kawirikawiri amatumphuka pakati pa iwo amene amadzipereka kutumikira. Ukuyenera kudzifunsa kuti, "Ndindani m'gulu ili amene ali ndi kuthekera kwa utsogoleri?" Zikhoza kukhala zofunikira kuti ufikire anthu ena paokha ndikukamba nawo kuti atsogolere m'maudindo ena.

Kuphunzitsa Atsogoleri

Pamene atsogoleriwa azindikiridwa, akuyenera kuphunzitsidwa. Uwu ndi udindo wa Mbusa aliyense wa Chipentekoste. Monga tanenera kale mbuyomu, Paulo ananenapo kuti ntchito ya Mbusa ndiyo "kuti akonzere oyera mtima kuntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu" (Aef. 4:12). Ukhoza kuchita izi munjira zitatu::

1. Kuwaphunzitsa pamene akugwira kale ntchitoyo. Utsogoleri wamtundu uwu umatchedwa kuti kuphunzira ntchito pogwira ntchitoyo. Abusa amapereka mtsogoleri watsopano kwa mtsogoleri wakale, wodziwa bwino ntchito yake. Mtsogoleri wakaleyu amayenda naye mtsogoleri watsopanoyu ndi kumamuphunzitsa m'mene angatsogolelere utumiki umene wapatsidwawo.

2. Msonkhano. Ukuyenera kuchititsa misonkhano ya apo ndi apo, mikumano kapena mibindikiro kumene atsogoleri atsopano aphunzitsidwe ntchito.

3. Kuthandizira. Ukhoza kufuna kuthandizira wina amene akuonetsa kuti ali ndi tsogolo pa utsogoleri. Kuti uchite izi, ukuyenera kutenga nthawi ndi atsogoleri amenewa kuwaphunzitsa utumiki. Izi ndi zimene Yesu anachita ndi akuphunzira ake. (Yohane 3:22). Anadzala ubwenzi wozama ndi iwo, kutsanulira moyo wake mwa iwo. Popita nthawi, anakhala ngati iye (Machitidwe 4:13). Yesu anafotokoza, "Koma yense, m'mene atakonzedwa mtima, adzafanana ndi mphunzitsi wake" (Luka 6:40).

KUDZALA MZIMU OGWIRA NTCHITO MOGWIRIZANA

Kuti mpingo uchite bwino, pakuyenera kukhala mgwirizano ndi cholinga chimodzi pakati pa anthu. Anthu adzimva kuti ali gawo la chinthu chachikulu kuposa iwo eni. Akuyenera kukhulupirira kuti mpingo wawo uli gawo la ntchito yayikulu ya chiombolo cha Mulungu ndipo kuti ukupezeka kuti utengepo mbali yofunikira mukukwaniritsa ntchitoyo

Izi ndi zoona kwa atsogoleri omwe si abusa. Kuti iwo adzipereke kwathunthu, akuyenera kumakhudzika kuti ali gawo lofunikira la gululi. Adzimva kuti akuyendera limodzi ndi anthu anzawo a malingaliro ofanana kuti akwaniritse mathelo olemekezeka. Monga Mbusa, ugwire ntchito yodzala mzimu wogwira ntchito mogwirizana pakati pa atsogoleri.

Khazikitsa Masomphenya Ofanana

Monga Mbusa wa pampingo, ndiwe osunga komanso olimbikitsa masomphenya a mpingo. Zitengera iweyo kuti ulele masomphenya ofanana m'mitima ya gulu la atsogoleri. Masomphenyawo akhale achikoka mokwanira kuti anthu afune kuwatsatira. Masomphenya a Yesu anali okopa kotero kuti Petro, Andreya,Yakobo ndi Yohane anasunthika nawo mpakana kusiya zonse ndi kumtsata iye (Mateyu. 4:18-22).

Mwanjira yomweyo, udzitha kufotokozera masomphenya momveka bwino komanso mokopa mtima. Pobwereza mawu a m'neneri wakale, udzitha kunena kuti, "Njira ndi iyi, yendani inu m'menemo" (fanizilani Yesaya 30:21). Monga mphamvu ya mtsinje wa ukulu, masomphenya amodziwa adzapangitsa kuti aliyense alowele njira imodzi.[1]

[1] Pa zambiri zokhudza kuponya masomphenya, onani Mutu 30: "Utsogoleri wa Masomphenya."

Pangitsa kuti anthu adzimva kulumikizana

Kuonjezera pa kudzala masomphenya amodzi pakati pa atsogoleri omwe si abusa, ukuyeneranso kukhazikitsa chimvanopakati pawo. Kuti anthu agwire ntchito limodzi bwino akuyenerakukondana zenizeni ndi kumamva kukoma pamene ali limodzi. Baibulo limatiuza kuti chifukwa chimodzi chimene Yesu anasankhira atumwi khumi ndi awiri chinali "kuti akhale ndi Iye" (Marko 3:14). Ndiye wina akhoza kuonjezera kuti, anawasankha iwo *kuti akhale ndi wina ndi mzake.* Pamene khumi ndi awiriwo amakhala ndi Yesu, komanso ndi wina ndi mzake, anafika pokondana wina ndi mzake. Limodzi anasanduka mphamvu yayikulu mdziko lapansi.

Mwanjira yomweyo, iwe monga Mbusa wa Chipentekoste, ukuyenera kukangalika kuti upange chimvano champhamvu pakati pa iwe, ogwira ntchito, komanso atsogoleri. Izi zikhoza kuchitika pakutenga nthawi kukhala pamodzi. Nthawi yokhala pamodzi ikhoza kuchitika munjira zitatu zozindikirika:

1. Nthawi yopemphera limodzi. Poyamba, iwe ndi timu yako ya atsogoleri muyenera kutenga nthawi kupemphera limodzi. Mukuyenera kukonza nthawi imene aliyense angamapezeke sabata iliyonse pamene limodzi ndi atsogoleri ako mudzipemphera limodzi. Nthawi yopempherayi idzilunjika ku cholinga chake. Chingakhale kuti nthawi itha kugwiritsidwa ntchito kupempherera zosowa zako, nthawi yochuluka izikhala yopempherera masomphenya ndi ma utumiki a pampingo.

2. Nthawi imodzi mu utumiki. Kenako, tengani nthawi limodzi ndi atsogoleri mu utumiki. M'mawa uliwonse musanayambe mapemphero, itanirani gulu la atsogoleri kupemphera ndi kuwakumbutsa iwo kuti mukugwira ntchito limodzi. Njira ina imene gulu la atsogoleri lingatumikilire limodzi ndi yakuti atsogoleriwa amapanga chikatikati cha gulu la anthu lokadzala mpingo.

3. Nthawi M'chiyanjano. Kachitatu, iwe ndi atsogoleri wamba muyenera kupeza nthawi yoyanjana limodzi. Atsogoleri anu akuyenera kulimbikitsidwa kumayenderana m'makomo mwawo. Kudya chakudya limodzi pamwezi kungachite zazikulumukulimbikitsa m'gwirizano wa chiyanjano pakati pa mabanja a gulu la atsogoleri anu. Yesu atatha nthawi yokwanira ndi akuphunzira ake, anati kwai wo, "Sinditchanso inu akapolo;… koma ndatcha inu abwenzi" (Yohane 15:15). Chimodzimodzinso, iwe ndi atsogoleri ako, mudzatha kutchulana wina ndi mzake, abwenzi.

Kuti mpingo uchite bwino, ukuyenera kukhala ndi mphata la atsogoleri wamba omwe ali odzipereka kupititsa patsogolo ntchito komanso masomphenya a mpingo. Mbusa wanzeru wa Chipentekoste, amakhazikitsa ngati limodzi la zolinga za utumiki wake kumanga gulu la mphamvu la atsogoleri omwe si abusa. Mwadaladala amayikiza nthawi ndi mphamvu zake mu kuzindikira, kusankha ndi kuphunzitsa atsogoleri wamba kuti atumikire nawo limodzi popititsa patsogolo ufumu wa Mulungu.

~ Mutu 34 ~

Kutsogolera Nthambi za Mpingo

Monga mwana amakulira m'mimba ya mayi ake, tsiku ndi tsiku thupi lake limakhala likumelera ziwalo zosiyanasiyana. Panthawi yomwe mwana amalengedwa m'mimba ya mayi ake, munthu watsopano amakhala ali dzira lomwe lapatsidwa moyo. Koma, chodabwitsa, chibadwa chomwe chimapangitsa kuti dzira lipangike kukhala munthu chimakhala chitakonzekeretsedwa kale. Pomatha ma ola makumi awiri mphambu zinayi (24), dzira lija limayamba kugawanikana mtizigawo tambirimbiri. Pokwana miyezi iwiri yoyambirira, ngakhale mwanayo amakhala wotalika macentimita khumi (10 cm) kapena mainchesi anai (4 inchesi), ziwalo zake zonse kuphatikizapo manja ndi miyendo zimakhala zilipo. Komabe, kuti mwanayo akwanitse kuchita zinthu monga munthu, ndi kukwanitsa kukhala kunja kwa m'mimba ya mayi ake, ziwalo zake zimasowekera kuti zikule. Pomatha miyezi isanu ndi umodzi potsatira itatuyo, mwana amakhala okonzeka kubadwa. Uyu ndi mwana wamtengo wapatali amene mayi ndi bambo ake ati amunyamule m'manja mwawo posakhalitsa. Nzosadabwitsa kuti David akondwera, "Chipangidwe changa nchoopsa ndi chodabwitsa" (Masalimo 139:14).

Mpingo ongodzalidwa kumene ukhoza kufanizilidwa ndi dzira limene langopatsidwa moyo kumene. Ndimpingo kale wachikhalire; komabe ukusowekera kuti ukhazikitse zinthu zina usanafike pozindikirika ngati thupi lochitachita la okhulupirira. Zina mwa zoti zikhazikitsidwe ndi monga nthambi za

mumpingo. Mutu uno ukamba za udindo wa Mbusa wa Chipentekoste mukukhazikitsa, kukuza, ndi kuyendetsa nthambi zimenezi.

CHOLINGA NDI KAGWIRIDWE NTCHITO KA NTHAMBI ZA MU MPINGO

Nthambi za mumpingo ndi mautumiki a pampingo omwe amakumana pamalo amene amakonzedwa kuti afikire zosowa za magulu a anthu osiyanayana pampingopo. Cholinga chake ndichakuti mpingo uthe kugwira bwino ntchito yake yofikira miyoyo yotayika ndikupanga ophunzira akhale chifanizo cha Khristu. Nthambi za mpingo zikhozanso kutengedwa ngati nsanamira zotchinjilizira thunthu la mpingo omwe ukukulirakulirabe. Pamene pali kuwonjezera nthambi zatsopano, kuthekera kwa mpingo kwakutumikira kumakula.

Cholinga cha Nthambi za Mpingo (Ma dipatimenti)

Kuti timvetsetse bwino cholinga ndi kagwiridwe ntchito kanthambi za pa mpingo, Mbusa wa Chipentekoste akuyenera kumvetsetsa poyamba ntchito ya mpingo. Mpingo unakhazikitsidwa ndi cholinga choti ulalikire uthenga wabwino kwa anthu amitundu yonse ndi kukwaniritsa lamulo lalikulu la Khristu. Kutuma Kwakukulu ndiko lamulo la Khristu lakuti "mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse" (Mat. 28:19). Lamulo loposa onse ndilo mayitanidwe a Ambuye kuti "uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi Mtima wako onse, ndi moyo wako onse, ndi nzeru zako zonse" ndi "Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini" (Mat. 22:37-39).

Maudindo ochuluka oterewa sangakwanitsidwe ndi Mbusa yekha ngakhale ogwira ntchito ya ubusa olipidwa. Ntchitoyi ndiyofunika manja ambiri. Nthambi za mu mpingo zinakhazikitsidwa kuti mpingo ukwanitse kufikira udindo wake wokhazikitsa ufumu wa Mulungu pa dziko.

Ntchito Zisanu ndi Ziwiri za Nthambi za Mpingo

Nthambi za mpingo zimathandizira mpingo kuti uthe kugwira ntchito zisanu ndi ziwiri:

1. Kufikira Otayika. Poyamba, nthambi za mpingo zinakhazikitsidwa kuti zithandizire mpingo kukwaniritsa lamulo la Khristu kuti "mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse" (Marko 16:15). Nthambi iliyonse mu mpingo itengepo gawo lake kumemeza mpingo kutchito

yofunikirayi. Akuyenera kulimbikitsa ma membala kuti aliyense atengepo mbali kugawa Uthenga Wabwino ndi ena ndi kuwatakasa kuti atengepo gawo kumbali ya zochitika zampingo pa usodzi ndi utumwi.

2. Kupanga Ophunzira. Yesu analamulira mpingo kuti "phunzitsani anthu a mitundu yonse… ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulani inu" (Mateyu. 28:19-20). Kuphunzitsa ndipo pamtima pa kupanga ophunzira. Maphunziro atsatanetsatane ali ofunikira kuti anthu akule m'moyo wauzimu komanso kukula kwa mpingo. Nthambi zimathandizira kukwaniritsa cholinga chimenechi.

3. Kulimbikitsa Kulambira. Mpingo unakhazikitsidwa ngati malo amene anthu a Mulungu akhoza kusonkhana ndi kumulambira Iye. "mumzimu ndi m'choonadi" (Yohane 4:23). Gulu loyendetsedwa bwino la mayimbidwe ndi malambiro lingathe kuthandiza kuti kulambira kotere kutheke.

4. Kupititsa Patsogolo Pemphero. Kuonjezera apo, mpingo ulipo kuti ulimbikitse ndi kuphunzitsa anthu a Mulungu kupemphera (Machitidwe 2:42). Yesu anati, "Nyumba yanga idzatchedwa nyumba yakupempheramo anthu a mitundu yonse" (Marko 11:17). Mpingo osonkhana pamalo ukuyenera kukhala malo amene Akhristu akweza mawu awo limodzi ndi kuyitanira pa Mulungu, kuyembekezera Iye kuyankha mapemphero awo (Mateyu. 18:19-20; Machitidwe 4:24). Nthambi zimathandiza mpingo kuti ukwaniritse ntchito imeneyi. Nthawi zonse zimene anthu amene ali gawo la nthambi akasonkhana mu mpingo, akuyenera kutsindika papemphero.

5. Kupereka Chiyanjano. Kuphatikiza apo, mpingo ulipo kuti upititse patsogolo chiyanjano pakati pa abale ndi alongo mwa Khristu. Nthambi zamu mpingo zimathandiza mpingowo kuti ukwaniritse cholinga chimenechi. Pamene anthu akukumana ngati mbali imodzi ya nthambi, amakula muchikondi pa wina ndi mzake. Zotsatira zake ndi zakuti amakhala okonzeka kuthandizana ndi kusamalirana mosavuta. Machitachita awa amathandizira kuyanjanitsa ndi kulimbikitsa thupi. Zimathandiziranso kukopa anthu atsopano kumpingo.

6. Kememeza kukachita utumwi. Mpingo ulipo kuti ukakwaniritse ntchito ya Mulungu. Unakhazikitsidwa kuti utenge Uthenga Wabwino wa Khristu kwa "anthu a mafuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse" asanabwerere kuchokera kumwamba (Mateyu 24:14; Chivumbulutso. 5:9). Nthambi zamu mpingo zimathandizira mpingo kudzikonzekeretsa okha kuti ukachite usodzi, kudzala mipingo, ndi kuchita utumwi.

7. Kukuza Atsogoleri. Chomaliza, Yesu adalamulira mpingo kuti uphunzitse atsogoleri. Analamulira akuphunzira ake kuti apite ndi kuphunzitsa akuphunzira (Mateyu 28:19). Pamene anakwera kumwamba, anapereka mphatso za utumiki ku Mpingo "kuti akonzekere oyera mtima kuntchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu" (Aefeso. 4:11). Paulo analangiza Timoteyo, "Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso" 2 Timoteo 2:2). Nthambi zamu mpingo zimathandiza mpingo kuti ukwanitse kugwira ntchitoyi moyenerera.

NTHAMBI ZIMENE ZINGATHE KUPEZEKA MU MPINGO

Pamene mpingo ukukula ndi kukhazikika, mbusa ndi gulu la atsogoleri ake motsogoza mapemphero muyenera kugawa utumiki mukayendetsedwe kake ka m'nthambi. Muyamba pokhazikitsa nthambi imodzi kapena awiri. Kenako monga m'mene Mzimu atsogozere, mukhazikitsa nthambi ndi madongosolo ena. Nthambi ndi ma utumiki amene mungakhazikitse ndi awa:

Maphunziro a Chikhristu

Chigawo cha Maphunziro a Chikhristu ndiye chiwalo choyambirira chophunzitsira cha mpingo. Nthambi imeneyi imakhazikitsidwa kuti ipange okhulupirira kukhala ophunzira pa kuwaphunzitsa mawu a Mulungu ndi kugwiritsa ntchito mfundo zake pamiyoyo yawo. M'mipingo yambiri ya Chipentekoste, maphunziro a Baibulo kapena Sande sukulu ndi mtima wa nthambi ya maphunziro a Chikhristu ndi utumiki oyambirira ophunzitsa akuphunzira pa mpingo. Ndipo kawirikawiri ndi nthambi yokhayo mumpingo imene imatumikira ku anthu a misinkhu yonse, kuyambira ana kufikira akuluakulu.

Mbusa wa Chipentekoste akuyenera kuyika patsogolo ntchito yokuza nthambi imeneyi. Ikuyenera kukhala nthambi yoyambirira pamene mpingo watsopano ukuyamba. Mpingo ungafunenso kukhazikitsa milaga kumene anthu amaumbidwa ndi kuphunzitsidwa mawu a Mulungu. Kuwonjezera apo, nthambi iliyonse ikuyenera kuchita nawo Maphunziro a Chikhristu pa mlingo wina wake.[1]

---

[1] Africa's Hope (omwe anasindikiza bukuli) analemba mabuku awiri amphamvu owumbira akuphunzira ku mipingo ya Chipentekoste mu Afirika. Loyamba ndi mndandanda wa mabuku wotchedwa *Kukhala Choonadi*, maphunziro a Sande Sukulu amene amaphunzitsa akuphunzira Baibulo onse muzaka zisanu ndi ziwiri. Lina ndi mndandanda wotchedwa *Mizu ya Chikhulupiriro*. Ili ndi buku la mitu ikuluikulu yokamba

Utumiki wa Amayi

Nthambi ya utumiki wa amayi ndi imodzi mwa nthambi zamphamvu kwambiri mu mpingo wa Chipentekoste. Cholinga chake ndicho kufikira amayi ndi Khristu ndikuwapatsa danga lachiyanjano ndi utumiki. Kudzera mu utumiki uwu, amayi amalimbikitsika kuti afikire mabanja awo, abwenzi awo, komanso anansi awo ndikuwabweretsa kwa Khristu. Amayinso amalimbikitsidwa kuti atenge nawo mbali pa kusula ophunzira, kudzala mipingo, utumwi ndi ma utumiki ena.

Utumiki wa Abambo

Nthambi ya utumiki wa abambo inakhazikitsidwa kuti ifikire abambo ndi uthenga wa Khristu, ndi kuwapatsa mwayi wachiyanjano cha Chikhristu ndi kuwabetchera kuti atenge udindo otsogolera m'mabanja awo komanso m'dera lawo. Kuwonjezera apo, utumikiwu ulipo kuti usokolotse abambo ku utumiki opatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera. Kudzera mu utumiki uwu, azibambo amabetcheredwa kuti atengepo mbali mu usodzi, kudzala mipingo, ndi zochita zina za paphata pa ntchito ya utumiki pa mpingo.

Utumiki wa Achinyamata

Cholinga cha nthambi ya utumiki wa achinyamata ndi kufikira achinyamata ndi uthenga wa Khristu ndi kuwakuza kuti akhale Akhristu amsinkhu ndi odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Komanso unakhazikitsidwa kuwaphunzitsa iwo kuti akhale moyo wa Umulungu, Kukhala moyo olemekeza Khristu, ndikuwamemeza ku utumiki waphindu kwa achinyamata anzawo.

Utumiki wa Ana

Cholinga cha nthambi ya utumiki wa ana ndikuwafikira ana ndi Khristu, kuwatsogolera iwo ku moyo odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndi kuwaphunzitsa iwo njira za Ambuye. Cholinga chake sikulowa m'malo mwa khama la makolo pakukuza anawo koma kuonjezerapo (Miyambo. 22:6). Kutambasuka kwa

za zinthu zofunikira zokhudza moyo wa Chikhiristu, monga, "Khwelero loyamba: Moyo wako watsopano mwa Khristu," "Ziphunzitso za Baibulo," "Moyo mu Mzimu" ndi ena ambiri. Mndandanda wa mabuku amenewa unasindikizidwa muzilankhulo zosiyanasiyana za mu Afirika. Mukhoza kupeza zambiri zokhudza zimenezi pa tsamba la intaneti la https://africaatts.org/resources/.

utumiki umenewu kumaphatikizapo mpingo wa ana ndi ma utumiki ena ophunzitsa ana monga magulu a anyamata ndi atsikana.

Kulambira ndi Kuyimba

Cholinga cha nthambi ya kulambira ndi kuyimba ndi kulemba ndi kuphunzitsa oyimba, atsogoleri akulambira ndi amakwaya kuti atsogolere anthu osonkhana kukulambira kodzozedwa ndi Mzimu (Yohane 4:23). Nthambi imeneyi imagwiranso ntchito ndi komiti yoyendetsa utumwi pokonza misonkhano ya usodzi komanso kudzala mipingo. Mamembala a gulu la matamando akuyenera kupemphera limodzi pafupipafupi komanso akuyenera kuphunzitsidwa m'mene angalandilire kupezeka kwa Mzimu ndi kutumikira mumphamvu yake.[2]

Utumiki wa Mapemphero

Gulu la mapemphero lopangidwa bwino ndi chigawo chofunikira mumpingo uliwonse wa Chipentekoste. Utumikiwu umapereka thandizo la uzimu ku mpingo pa kupembedzera abusa ake ndi ma membala omwe. Limapembedzeranso iwo amene sanapulumutsidwe, kumudzi kuno, angakhale ndi mu Afirika yense komanso dziko lonse la pansi. Utumikiwu umatenga maonekedwe osiyanasiyana; monga nkumano wa nthawi zokhazikika, msonkhano wa mapemphero kapena kupemphera mukuyenda, magulu amapemphero, komanso utumiki wadziphona dzapemphero.[3]

Nthambi ya Utumwi

Nthambi ya utumwi ili ndi udindo oonetsetsa kuti mpingo ukuyika chidwi pa kufalitsa uthenga wabwino kwa anthu onse kulikonse. Udindo wake umaphatikizapo kukonza dongosolo komanso misonkhano yosodza anthu ndi kudzala mipingo. Misonkhano yosodza anthu ikuphatikizapo misonkhano ya chitsitsimutso, misonkhano yolalikira pabwalo, kuyenda khomo ndi khomo

[2] Utumiki wa kulambira pa mpingo wafotokozedwa mwatsatanetsatane mu Mutu 18: "Kutsogolera Mpingo M'kulambira."

[3] Pa zambiri zokhudza utumiki wa pemphero pa mpingo, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

kuchitira umboni, kugawa zolemba za mau a Mulungu, ndi njira zina zopangidwa.[4]

Nthambiyi ilinso ndi udindo okuza ndi kupititsa patsogolo machitachita a utumwi pa mpingo. Kudzera mudongosolo lofunikilali, mpingo umamemedwa kuti uthandize atumwi pakuwapempherera komanso kupereka ndalama. Utumiki umachita izi, pophunzitsa anthu za cholinga cha Mulungu ndi kuwaonetsa atumwi. Mipingo ina ingafune kukhala ndi nthambi zapazokha monga usodzi, kudzala mipingo ndi utumwi.[5]

Utumiku wa Zachifundo

Yesu ankakhudzika ndi zosowa za kuthupi za wanthu. Mpingo weniweni wa Chipentekoste umachita chimodzimodzi. Yakobo analemba, “Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: kucheza ndi ana amasiye ndi akazi amasiye m'chisautso chao, ndikudzisungira mwini wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi” (Yakobo 1:27). Kudzera mu utumiki wa zachifundo, Mpingo wa Chipentekoste umatambasula dzanja la Khristu kwa anthu osowa ndi opwetekeka.[6]

Utumiki wa Anthu Akulu Osakwatiwa

Kudzera mu utumiki wa anthu wosakwatiwawu, Akhristu omwe ali paokha amapatsidwa kuthekera kokula mphamvu mu chikhulupiriro chawo kusakhala chete mumachitachita a mpingo. Utumiki uwu umathandiza mpingo kuti uzindikire phindu lokhala ndi akulu akulu omwe ali paokha kutenga nawo mbali muzochitikachitika za mpingo. Umafuna kupindulapo pa kuthekera kwakukukulu kumene sikumalabadilidwa m’gulu limeneli nthawi zambiri.

Utumiki wa Ana a Sukulu za Ukachenjede (Univesite kapena Koleji)

Ngati mpingo wanu uli pafupi ndi sukulu ya ukachenjede kapena yosula maluso osiyana siyana, mulingalire pakupemphera zokhazikitsa utumiki wa ana a

[4] Pa zambiri zokhudza kumemeza mpingo kuti ufikire anthu otayika, onanani Mutu 37: “Kulalikira Otayika.”

[5] Kuti mudziwe zambiri pa kukuza dongosolo la mpingo la utumwi, onani Mutu 40: “ Kukhazikitsa Dongosolo la Utumwi la Mpingo Wapamalo”

[6] Kuti mudziwe zambiri pa utumiki wa chifundo, onani Mutu 38: “Kutumikira dera lanu.”

kusukuluzo. Cholinga cha utumiki umenewu ndi kufunafuna kufikira sukuluzi ndi kupindula miyoyo ya ophunzira kwa Khristu. Utumiki uwu udzaphunzitsa ndi kumemeza ophunzirawa kuti afikire ophunzira ochuluka ndi Uthenga Wabwino. Ngati mpingo wanu uli ndi Nthambi ya utumiki wa m'masukulu a ukachenjede, muyenera kugwira ntchito moyanjana ndi bungwe limenelo.[7]

Njira Zofalitsira Uthenga Zamakono

Nthambi ya zofalitsa mauthenga pogwiritsa ntchito njira zamakono imaona zonse zokhudza kafalitsidwe kauthenga mnjira zamakono. Imakhazikitsa, kugwira ntchito ndi kusamalira kamvekedwe ka mawu ndi zida zakanema pa mpingo. Nthambi imeneyi imasindikizanso ndi kuyang'anira webusaiti ndi tsamba la mchezo kuti zizipezeka pa makina a intaneti. Nthambiyi imagwiranso ntchito yosindikiza misonkhano ya mpingo ndi zochitika zina kudzera mu mawailesi, makanema, komanso pa makina a intaneti.

Othandizira ndi Kulandira Alendo

Cholinga cha nthambi yothandizira ndi kulandira alendo ndi kulandira ndi kuthandizira iwo amene abwera ku zochitika zampingo. Utumiki umenewu umayesetsa kulenga malo achifundizi ndi kumva kulandilidwa kwa onse. Gulu limeneli limalandira obwera kudzakhala nawo komanso kulondolera alendo kumalo awo, kugawa zina ndi zina zoti anthu apatsidwe, ndi kutolera chopereka. Amapititsa patsogolo chitetezo, kuthana ndi zosokoneza ndi kusungitsa bata mumpingo.

Azomanga manga ndi Pabwalo

Nthambi ya zomangamanga ndi kuona pabwalo ili ndi udindo okonza ndi kusamalira katundu wa mpingo. Imaonetsetsa kuti mkati ndi kunja kwa nyumba kuli kwa ukhondo komanso kokonzedwa bwino.

KUKHAZIKITSA NTHAMBI

Funso ndilakuti, "Kodi mbusa wa Chipentekoste angakhazikitse bwanji nthambi ndi mautumiki atsopano pa mpingo?" Inde, ndi zosatheka kuyambitsa

[7] Zofunikira pakukhazikitsa utumiki wa ana asukulu za ukanjede mukhoza kuzipeza pa tsamba la intaneti https://chialpha.com/resources/.

nthambi zonse zatchulidwa pamwambapa nthawi imodzi. Komano nthambi zatsopano zikuyenera kukhazikitsidwa motsogozedwa ndi pemphero komanso mwadongosolo. Kuyambitsa nthambi zatsopano kudzitengedwa ngati ntchito yoyichita kwa zaka zingapo pang'ono pang'ono khwelero limodzi panthawi.

Kuyambitsa nthambi kapena utumiki watsopano nthawi zambiri kumatengera kulimba mtima pachikhulupiriro kwa Mbusa komanso atsogoleri a mpingo. Akuyenera kuona chosoweka, amve chitsogozo cha Mzimu, kenakano mwachikhulupiriro akhazikitse utumiki watsopano.

Kuyamba Zochitika

Inu pamodzi ndi gulu la atsogoleri muyambe dongosolo pofunafuna Mulungu. Mumupemphe iye, "Ambuye, ndi ma utumiki ati atsopano amene akufunika mumpingo nthawi ino?" Mukhozano kulemba mndandanda wa nthambi ndi ma utumiki amene mukuona kuti Mzimu akukutsogolerani kuti muyambe. Mutatha kulemba mndandanda wanu, muyale kuti muyambira nthambi kapena utumiki uti, nanga otsatira wake ukhale uti mpakana omalizira.

Kenakano muyike chidwi chanu ku nthambi imene mwayisankha kuti ikhale yoyambirira. Mukhale pansi ndi atsogoleri anu ndi kukambirana izi:

- Titsate ndondomeko yanji kuti tiyambitse nthambi yatsopanoyi?
- Ndizinthu zanji zimene zifunikire?
- Ndindani amene atsogolere ndi kuyendetsa dongosolo limeneli?
- Iyambe liti?

Mukuyenera kulemba zisankho zanu ndikupitirira kuzipempherera. Kenako, nthawi mukaona kuti yakwana, yambani kukhazikitsa dongosolo lanu lija. Mukulangizidwa kuti muyambe mochepa, pogwiritsa ntchito zipangizo zomwe muli nazo. Mwachitsanzo, ngati mukufuna kuyambitsa nthambi yatsopano ya Maphuziro a Baibulo a Lamulungu, mukhoza kuyamba ndi makalasi atatu: ya akuluakulu, ya achinyamata ndi ya ana. Mukhoza kumuyika wina akhale mtsogoleri kapena mukhoza kutenga nokha udindo umenewu koyambirira kuno. Pamene utumikiwu ukukula, mukhoza kukhazikitsa makalasi ena ndi kusankha atsogoleri atsopano.

Kusankha Atsogoleri

Chifungulo cha chipambano pa nthambi ya utumiki yatsopano ina iliyonse ndi atsogoleri osankhidwa komanso kuphunzitsidwa bwino. Posankha atsogoleri, mudziyang'ana anthu amene ali ndi kuthekera kwa utsogoleri, iwo amene mungawaumbe kukhala atsogoleri. Atsogoleri amenewa akhale "odzala ndi Mzimu ndi nzeru" (Machitidwe 6:3). Kuonjezera apo, akhale odzala ndi chikhulupiriro, komanso alandire masomphenya a mpingo.

Kuphunzitsa Ogwira ntchito

Kawiri-kawiri, atsogoleri okhala ndi zowayenereza samapezeka. Potero, Mbusa ochitachita akuyenera nthawi zonse kumaphunzitsa/kukuza atsogoleri atsopano. Izi ndi zomwe Yesu anachita. Ndipemphero anasankha amuna khumi ndi awiri amene anawakuza akhale atumwi (Luka 6:12-13). Chingakhale anali anthu wamba, Yesu anaona kuthekera kwa utsogoleri mwa iwo. Anawaitana, "Tiyeni pambuyo panga…ndidzakusandutsani asodzi a wanthu" (Mateyu. 4:19). Pamene amamutsata iye, anawaumba kukhala atsogoleri.

Pamene mukusankha atsogoleri ndi ogwira ntchito atsopano a nthambi zosiyasiyana ndi zofunikira kuwalonjeza maphunziro. Awuzeni anthu "tiyenda nanu limodzi kukuphunzitsani m'mene mungakwanilitsire ntchito ya utumiki wanu." Maphunziro a utumiki amenewa angathe kuchitidwa m'njira zosiyanasiyana: kudzera m'misonkhano, kuphunzitsa m'modzi m'modzi pomukuza pa utumiki, ndi njira zina zotchakuka bwino. Ngati mpingo ungakhale ndi atsogoleri okonzeka kutumikira nthawi zonse, abusa achite mwadaladala kuphunzitsa atsogoleri atsopano.[8]

Kulenga Mzimu ogwirira ntchito limodzi pa gulu

Kuti nthambi zichite bwino pa mpingo, mukuyenera kulenga kukhala ndi cholinga ndi kudzipereka pakati pa atsogoleri ndi ogwira ntchito. Mzimu ogwira ntchito pamodzi udzatakasa anthu kuti agwirire ntchito limodzi ndi kudzipereka kwathunthu pantchito yawo kuti ayigwire bwino. Mukhoza kuchengetera mzimu ogwirira ntchito limodzi pakumawakumbutsa pafupipafupi za masomphenya a mpingo, ndi kuwaonetsera kufunikira kwa udindo wawo mukukwaniritsidwa kwa masomphenya.

[8] Pa zambiri zokhudza kuphunzitsa anthu ku utumiki kumpingo wakudera, onani Mutu 33: "Kusonkhanitsa Atsogoleri Omwe si Abusa"

Mudzikumana pafupipafupi ndi atsogoleri omwe akuyendetsa nthambi zosiyanasiyana ndi otumikira ndi kuwalimbikitsa iwo agawane zigonjetso ndi zipambano. Mudzizindikira pagulu ogwira ntchito mokangalika ndi kuwalemekeza iwo pa zimene akwaniritsa (Aroma. 13:7).

Nthambi za mumpingo zimatenga udindo ofunikira mukuthekera kwa mpingo wa Chipentekoste kukwaniritsa Kutuma Kwakukulu kwa Yesu ndi Lamulo Lalikulu. Mbusa ochitachita adzakangalika kukhazikitsa nthambi za utumiki mu mpingo wake.

~ Mutu 35 ~

Kuyang’anira Umembala wa Mpingo

Tangoganizirani pa sukulu ya boma imene palibe chodziwitsa kuti mwana wasukulu ndi uti nanga amene saphunzira pamenepo ndi uti. Sukulu yoti ilibe mndandanda wakalembera wa ana asukulu ndipo sisunga kalembera wa m’mene ana amakhozera pasukuluyi. Nzodziwikratu kuti sukulu yotereyi singakhale ndi mwayi waukulu opambana. Izi zikhozanso kukhala chomwechi ngati zitachitika pa mpingo. Mpingo umene ulibe dongosolo lozindikira kuti ndindani amene ali membala kapena ayi, komanso osatha kutsatira bwino m'mene moyo wa uzimu wa mamembala ake ukuyendera, sungakule kukhala mpingo wamphamvu.

Monga Mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kuonetsetsa kuti mpingo umene mukuwutsogolera ukuyang’aniridwa bwino. Dera limodzi limene liyenera kusamalidwa bwino ndilo la mndandanda wa mamembala. Kalembera oyendetsedwa bwino wa mamembala amathandizira kuti mpingo uthe kukwaniritsa bwino udindo wake opatsidwa ndi Mulungu kusamalira nkhosa ndi kulalikira otayika. Mutu uno ukuyang’ana udindo oyang’anira chiwerengero cha mpingo.

ULAMULIRO WA M'BAIBULO OSAMALIRA CHIWERENGERO CHA MA MEMBALA

Ngakhale kuti Baibulo sililankhula mwachindunji pankhani yokhala membala mkaundula wa mpingo monga m'mene ziliri m'mipingo lero, koma limagwirizana nalo ganizo limeneli.

Maziko a Baibulo pa nkhani ya umembala

Nkhani yomasunga chiwerengero cha mamembala a mpingo gwero lake ndi Chipangano Chakale. M'menemo Mulungu anapangana ubale wapaderadera ndi fuko la Israele. Anali anthu ake, ndipo iye anali Mulungu wawo. Mchipululu, Mulungu anayambitsadongosolo lakayang'aniridwe ka anthu ake. Analamulira Mose, "Werenga khamu lonse la ana a Israele, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba ya makolo ao ndi kuwerenga maina ao, amuna onse mmodzimmodzi" (Num. 1:2). Mose ndi Aroni kenako anagwiritsa ntchito kalemberayu kusankha anthu amene angatsogolere, kutumikira ndi kuteteza anthu a Mulungu.

Mu Chipangano Chatsopano, Stephano anayankhula za Israele monga "Msonkhano (Mchihelene: *Ekelezia*) mchipululu." Mchipangano Chatsopano mawu akuti *Ekelezia* anawamasulira kuti "mpingo." Amafotokoza za msonkhano kapena khamu la anthu loyitanidwa kutuluka m'dziko lapansi kutsata Khristu ndi kupititsa patsogolo ntchito yake pano padziko lapansi.

Yesu analengeza "ndidzamanga mpingo wanga" (Mat. 16:18). Anayamba kuchita dongosolo limeneli poitana anthu kuti amtsate Iye (Mat. 4:19). Kuchokera mwa omutsatira amenewa, Yesu anasankha ena kukhala atumwi (Marko 3:13-14). Atumwi amenewa nawonso anasankha ena kukhala madikoni kuti atumikire pansi pawo. Amayika dongosolo kuti mpingo upite patsogolo. Zotsatira zake, "chiwerengero cha akuphunzira chinachuluka kwakukulu M'yerusalemu" (Mach. 6:1-7).

Kuti mpingo wakudera uchite bwino, ndikofunikira kuti aliyense adziwe kuti membala ndi uti nanga amene simembala ndi uti. Mpingo oyamba unazindikira ichi. Kwa iwo, panali kudziwika bwino kuti membala ndi ndani ndipo amane simembala ndi uti. Mwachitsanzo, panthawi ina yake, Paulo analangiza mpingo wa ku Akorinto kuti achotse mukaundula wampingo m'bale amene amachimwa

(1 Ako. 5:5, 13). Kaundula oyendetsedwa bwino adzathandiza Mbusa kulimbikitsa okhulupirira ndi kupititsa patsogolo ntchito ya mpingo.

M'mene Baibulo Limakambira za Umembala

Wina asafanizire za umembala wamumpingo ndi umembala wa gulu la chikunja. Zimapita kwa kuya kuposera apa. Paulo akufanizira mpingo ndi thupi la munthu, kulitchula kuti "thupi la Khristu" (1 Akorinto. 12:27). Membala aliyense wa mpingo potero ali chiwalo cha thupi la Khristu ndipo "membala aliyense ali wa ena onse" (Aroma. 12:5). Monga m'mene thupi linapangidwira, ndipo chiwalo china chilichonse chili ndi ntchito yake, chimodzimodzinso mpingo wa Khristu.

ZOYENEREZA ZA UMEMBALA

Muchipangano chakale, Mulungu anakhazikitsa milingo yoti anthu ake atsatile pamoyo wawo. Milingo imeneyi inatchulidwa mwachidule mu Malamulo Khumi (Eksodo 20:1-17). Chimodzimodzinso, m'mene mpingo oyamba unakula ndikumwazikira kupyola M'yerusalemu, Atumwi amatsogozedwa ndi Mzimu Woyera kukhazikitsa zowayenereza amitundu kuti akhale gawo la mpingo (Machitidwe 15:19-20, 28-29). Monga Mbusa wa mpingo wa Chipentekoste, ukuyenera kuonetsetsa kuti aliyense amene walandiridwa mumpingo kukhala membala akukwaniritsa zoyenerera zina, kuphatikizapo izi:

Kubadwa Kwatopano

Mpingo wakudera ukhale chithunzithunzi cha mpingo wadziko lonse. Mpingo wadziko lonse umaphatikizapo anthu onse amafuko osiyanasiyana amene ayika chikhulupiriro chawo mwa Yesu Khristu ndipo apulumutsidwa. Umaphatikiza okhawo amene abadwadi mwa Mzimu Woyera (1 Akorinto 12:13). Potero, munthu asanakhale membala wa mpingo wa kudera, ayambe kaye wakhala membala wa mpingo wadziko lonse. Ambuye mwini adzikhala kuti wa waonjezera yekha kumpingo wake (Machitidwe 2:47). Zimatsatira chonchi, kuti munthu akhale membala wa mpingo wa kudera, akuyenera kukhala obadwadi mwatsopano zenizeni (Yohane 3:3-7).

Ubatizo Wa Madzi

Choyenereza chachiwiri ndicho ubatizo oviikidwa m'madzi. Yesu akulamula kuti "mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la

Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera" (Mateyu 28:19; onaninso. Mach. 2:38). Ubatizo wam'madzi ndi umboni wa pagulu kuti wina wachokera kuimfa, kulowa kumoyo (Aroma 6:4).[1]

Chikhulupiriro Chimodzi

Choyenereza chotsiriza kuti munthu ukhale membala ndicho kugwirizana kwathunthu ndi ziphunzitso ndi mfundo za mpingowo (Onaninso 1Akorinto. 1:10). Choyenereza ichi chimaonetsetsa kuti mpingo ukhale ogwrizana ndi wachindunji kuntchito yopatsidwa ndi Mulungu. Zinthu izi ziphunzitsidwe ku kalasi ya mamembala atsopano.

KULANDIRA MA MEMBALA ATSOPANO

Monga Mbusa, ukuyenera kuonetsetsa kuti mpingo ulindindondomeko yolongosoka yolandilira mamembala atsopano. Ndondomekoyi ikhale ndi zinthu zitatu:

Kulimbikitsa Umembala

Mudzilimbikitsa kawirikawiri amene angokhulupirira kumene kuti alowe mpingo wanu. Kuti muchite izi, muzitenga nthawi pamene mukuchita mapemphero kufotokozera ubwino okhala membala wa mpingo ndi kumema Akhristu atsopano kuti akhale mamembala. Mungathenso kuyankhula kwa aliyense payekha amene akhoza kukhala membala wanu. Mchitidwe uwu udzaonetsetsa kuti nthawi ndi nthawi mamembala atsopano akuonjezeredwa kumpingo wanu. (Apapa tikuyerekezera kuti anthu atsopano akumabwera kumpingo wanu chifukwa cha misonkhano yolalikira kwa otayika imene mpingo wanu ukuchita.[2]) Kuphatikiza apo, mudzionetsetsa kuti mafomu a umembala alipo nthawi zonse.

Kukonzekera Umembala

Ndizofunikira kuti mpingo wanu ukhale ndi njira zokonzekeretsa anthu kukhala ma memembala. Imodzi mwa njira izi ndi kudzera mumakalasi a

[1] Pa zambiri zokhudza ubatizo wa madzi, onani Mutu 42: "Kuchititsa Masakramenti, Kudalitsa Ana, ndi Kukhazikitsa Atsogoleri."

[2] Pazambiri zokhudza kufikira otayika, onani Mutu 37: "Kulalikira Otayika."

umembala. Iyi ikuyenera kukhala kalasi yosalekeza, yoti ena akamamaliza ena akuyamba. Ikhoza kumachitika m'mawa nthawi ya maphunziro a Baibulo (Sande sukulu) kapena nthawi ina iliyonse yoyenera. Mukalasi imeneyi, iwo amene akufuna kukhala mamembala aphunzitsidwe phindu ndi udindo wa membala wa mpingo. Zambiri mwazimene takambirana pa mutu uno zikhoza kuphunzitsidwa mukalasi limeneli.

Kulandira Mamembala

Pamene akulu otsogolera mpingo awavomeleza, mamembala atsopano alandiridwe mumpingo mwachimwemwe pa mwambo umene aliyense akhale nawo patsiku la mulungu losankhika. Anthu omwe amaliza maphunzirowa ayimitsidwe kutsogolo kwa mpingo. Ndiye muwalandire monga mamembala atsopano ndi kuwapempherera iwo. Mpingo kenako utambasule "dzanja la chiyanjano" (Agal. 2:9). Panthawi iyi mupereke chiphaso kwa membala aliyense watsopano. Pamenepono mulembe mayina awo pa ndandanda wa mamembala a mpingo.

Kuphatikiza apo, ndizabwino kuti wina wa abusa akayendere mamembala atsopanowa m'makomo awo. Izi ziwathandizira iwo kuti adziwe m'mene mpingo ukuyamikira chisankho chawo. Pomaliza, mulumikizitse mamembala kumautumiki a pampingo, monga milaga, utumiki wa amayi, utumiki wa abambo, utumiki wa achinyamata ndi ena.

UDINDO WA UMEMBALA

Monga Mbusa wa mpingo, udzionetsetsa kuti mamembala akudziwitsidwa za udindo wawo komanso mwayi umene alinawo pokhala membala.

Udindo wa Membala ku Mpingo

Kukhala membala pampingo kumabwera ndi udindo. Udindo umenewu umaphatikizapo zinthu izi:

1. Kusajomba chisawawa kumpingo. Olemba buku la Ahebri anachenjeza Akhristu kuti asanyalanyaze kusonkhana kwawo pamodzi. M'malo mwake, iwo amayenera kumakumanandikulimbiktsana wina ndi mzake. Izi zinali zofunikira kwambiri makamaka pounikira kuti Yesu akudza posachedwa (Ahebri. 10:25). Chimodzimodzinso, mamembala a mpingo lero akuyenera kukhala okhulupilika kumikumano yawo ya pampingo. Kumeneko, akalimbikitsidwa, kulambira

Mulungu, kupemphera limodzi, kulandira chiphunzitso, kupereka kuntchito ya Ambuye, ndikupanga maubale okhazikika ndi Akhristu ena odzipereka.

2. Kuyenda M'moyo odzazidwa ndi Mzimu. Membala aliyense wampingo wa Chipentekoste akhale odzipereka kuyenda m'moyo odzazidwa ndi Mzimu (Agalatiya. 5:25). Ngati sanabatizidwe ndi Mzimu Woyera, afunitsitse kulandira (Mach. 1:4-5; Aef. 5:18). Ngati adzazidwa ndi Mzimu, akuyenera kukhala odzipereka kupitilira kuyenda m'moyo odzazidwa ndi Mzimu (Agal. 5:16, 25).[3]

3. Kukhala Mboni Kosalekeza. Membala aliyense akuyenera kukhala mboni ya Khristu (Mach. 1:8). Akuyenera kugawana nawo Khristu apabanja pawo, abwenzi, anansi ndi ogwira nawo ntchito. Yesu anatilamulira ife, "Chomwecho muwalitse inu kuunika kwanu pamaso pa anthu, kuti pakuona ntchito zanu zabwino, alemekezeAtate wanu wa Kumwamba" (Mateyu. 5:16).

4. Kukhala m'chiyero. Njira imodzi imene Mkhristu wa Chipentekoste amachitira umboni wa Khristu ndikukhala moyo wachiyero (1 Petro. 1:15; 2:9). Pakuchita ichi, anawonetsera chikondi chawo pa Mulungu. Panthawi yomweyo, miyoyo yawo imachitira umboni pazimene zimatanthauza kukhala ophunzira wa Khristu (Afil. 2:15).

5. Kupereka mokhulupirika. Membala wina aliyense wa mpingo akuyenera kuthandizira mokhulupirika muzachuma (1 Ako. 16:2). Pakupereka zakhumi zawo ndi zopereka amalimbikitsa thupi la Khristu ndi kuthandiza kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu padziko la pansi. Kuonjezera apo, kupereka mokondwera kumamkondweretsa Mulungu ndipo amatsegula zipata za madalitso ake pa miyoyo yawo (2 Ako. 9:7-8; Luka 6:38).

6. Machitachita akutumikira. Kupitilira apo, membala aliyense akuyenera kupeza malo ake oti adzitumikira mu mpingo. Pamene membala aliyense akuchita mbali yake, mpingo umakhala wa mphamvu. Monga Mbusa, uyenera kuyesetsa pakuwonetsetsa kuti membala aliyense azindikire mphatso zake zapaderadera ndikuti adzipereke kuzigwiritsa ntchito kutumikira Khristu ndi mpingo wake.

7. Kulimbika M'pemphero. Chizindikiro chodziwika bwino cha mpingo weniweni wa Chipentekoste ndicho kukangalika mupemphero. Membala aliyense

---

[3] Pa zambiri zokhudza kutsogolera okhulupirira mu kuyenda odzazidwa ndi Mzimu, onani Mutu 11: "Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekosite" ndi Mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

akuyembekezeka kupempherera kawirikawiri abusa, mpingo, dera lake, ndi mamembala ena a mpingo. Mukhoza kufuna kulimbikitsa ena kuti akhale mugulu la opembedzera.

8. Mtima umodzi. Pomaliza, mamembala akuyembekezereka kukhala ogwirizana. Mtima oterewu udzabweretsa umodzi pa mpingo (Aef. 4:3). Udzaonetsetsa kuti mpingo sukusokonezedwa ndi kusamvana pazinthu zachabechabe, ndi kukhala wa chindunji pakukwaniritsa ntchito imene Mulungu anaupatsa.

Udindo wa Mpingo ku Mamembala

Simamembala okha amene amakhala ndi udindo pa mpingo, mpingonso nawo umasenza udindo pa mamembala ake. Udindoumenewu ndi kuphatikizapo zinthu izi:

1. Kulandilidwa mwansangala. Poyambirira, mudzionetsetsa kuti mamembala atsopano akulandiridwa mwansangala ndi kukhala gawo ndi mbali ya zochitika pa mpingo. Ena amakhala kuti asiya anthu ndi zinthu zomwe anazizolowera. Alowa mudziko latsopano limene sakulidziwa bwinobwino. Muonetsetse kuti mamembala amenewa athandizidwa kuti asinthe ndi kuyamba kuzolowera zowazungulira zatsopano zimene apezekamo. Muchite chothekera chilichonse kuti anthu amvedi kuti iwo ndi anadi a m'banja la Mulungu.

2. Mwambo wapamwamba wa Mapemphero. Chachiwiri, monga Mbusa, muli ndi udindo kwa mamembala atsopano ndi akale omwe kuwapatsa mwambo wa mapemphero omangilira ndithu. Mwanjira ina, udzionetsetsa kuti mwambo wa mapemphero ndi wapamwamba ndiponso wakonzedwa bwino lomwe. Kuti izi zitheke, udzichita zotheka ndi kukonzekera kulalikira uthenga olamitsa ndi otakasa anthu. Udzionetsetsa kuti gawo lililonse la mapemphero likuchitidwa bwino, molemekezeka komanso mwaukadaulo. Izi ndikuphatikizapo kulambira, kupereka, zolengeza ndi gawo lina lililonse la mwambo wa mapemphero. Powonjezera apo, inu pamodzi ndi atsogoleri mudzipemphera mwakathithi kuti pa mwambo wanu wa mapemphero Mzimu Woyera apezeke mwamphamvu.[4]

[4] Kuti muunikiridwe zambiri zokhudza kakonzedwe ka mwambo wa mapemphero, onani Mutu 18 "Kutsogolera Mpingo M'kulambira."

3. Chisamaliro chaubusa. Komanso, monga Mbusa wa nkhosa, ulindi ntchito yoonetsetsa kuti membala aliyense akutengedwa kuti ndiwofunikira komanso kuti akusamalidwa. Udzitengera Yesu amene ananena kuti ndi "Mbusa wabwino… amene ataya moyo wache chifukwa cha nkhosa" (Yohane 10:11). Ukonzekere kutumikira angakhale mamembala a mpingo apansi (Luka 15:1-7).[5]

4. Pemphero loona Mtima. Chotsatira, monga Mbusa wa Chipentekoste, udzipempherera mamembala ako a mpingo.Zingakhale bwino kuti ukhale ndi m'ndandanda wa maina awo kuti ukhale ngati mlozo popemphera. Ukhozano kugwiritsa ntchito m'ndandandawo kupemphera tsiku ndi tsiku kupempherera membala aliyense. Kupitilira apo, munthawi ya chipsinjo, iwe ndi atsogoleri ako mukonzekere kuyendera mamembala amene apwetekeka ndi kuwalimbikitsa ndi kuwapempherera iwo.[6]

5. Chiphunzitso cha Baibulo. Komanso, monga Mbusa wa Chipentekoste okhulupirika, udzionesetsa kuti mamembala ako a mpingo alandira chiphunzitso cholamitsa. Chiphunzitsochi chidzikhala chofunikira chopatsa anthu zochita pa moyo wawo. Chidzawathandiza iwo kukula ndi kukhala okhwima mu uzimu. Udziyang'aniranso chiphunzitso cha ku maphunziro a Baibulu (sande sukulu) ndi kumilaga kuti chikhale cholamitsa ndi chomangilira.[7]

6. Chitetezo kwa aneneri Onyenga. Monga Mbusa, uli ndi udindo oyang'anira nkhosa za Mulungu ndi kuziteteza ku aneneri ndi aphunzitsi onyenga (Onaninso Machitidwe 20:28-29). Njira imodzi imene mungachitire izi ndikuphunzitsa choonadi cha mawu a Mulungu. Njira ina ndipakuwatchula aneneri ndi aphunzitsi onyengawo, kuonetsera kulakwika kwa njira zawo. Kupitilira apo, ukhoza kuteteza mamembala ako ku aneneri onyenga posalola "mimbulu mchikopa cha nkhosa" imeneyi kuti itumikire pagome lako (Mateyu. 7:15).[8]

---

[5] Onani Mutu 24: "Kusamalira Nkhosa."

[6] Pa zambiri zokhudza Mbusa wa Chipentekoste ndi pemphero, Onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero."

[7] Pa zambiri zokhudza Mbusa wa Chipentekoste ngati mphunzitsi, onani Mutu 17: "Kuphunzitsa Kwabwino." *Kukhala Choonadi* ndi *Mizu ya Chikhulupiriro* ndi maphunziro abwino kwambiri ophunzitsira a chipentekosite. Zikupezeka ku Africa Theological Training Service (ATTS) pa https://africaatts.org/resources/.

[8] Pa zambiri zokhudza kuteteza mpingo ku aneneri onyenga, onani Mutu 27: "Kuteteza Nkhosa."

7. Mwayi otumikira. Mudziwapatsakonso mpata mamembala atsopano otumikira mumpingo. Muwapatse danga lothazirapo mwachangu pazinthu zina zazing'ono. Izi zithandizira kuwamangilira iwo kumpingo. Ziwathandiziranso kumvetsetsa pachiyambi pomwe kuti kutumikira Mulungu kuposa kusonkhana nawo pazochitika pa mpingo. Zimakhudzanso kutenga nawo mbali.

8. Kumanga ma ukwati ndi kuyikitsa Maliro. Potsiliza, monga Mbusa wawo, muli ndi udindo oyenda ndi mamembala kudzerakuzochitika zosanduliza miyoyo yawo. Mudziwapatsa uphungu wa pabanja ndikudalitsa ma ukwati wawo. Mudziyikitsanso maliro ndikuthandizira polimbikitsa oferedwa.[9]

MISONKHANO YA MAMEMBALA

Nkumano wa mamembala ndi gawo limodzi lofunikira pa moyo wa mpingo wa Chipentekoste. Mumisonkhano imeneyi, mamembala amabwera pamodzi ndi kumakambirana zochitika mumpingo. Kumeneku, abusa ndi atsogoleri ena amagawana malipoti okhudzana ndi mmene mpingo ukuyendera, zobetchera ndi zosoweka. Mkumano wa mamembala udzichitika chaka ndi chaka.Kuphatikaza apo, misonkhano yapadera idzikonzedwa ngati kukusowekera kutero.

Misonkhano ya mamembala imakhala nthawi yabwino yokambirana zochitika zimene zikubwera ndi kugawana nawo mpingo masomphenya ako. Misonkhano iyi imaperekanso mwayi kwa mamembala kukambirana zomwe akuyembekezera ndi maloto awo pa msonkhanopo. Mukuyenera kugwiritsa bwino ntchito misonkhano yotereyi. Mukhoza kuchita izi pokonzekera bwino. Nthawi zonse mudzibwera ku misonkhano yotereyi ndi mndandanda wokonzedwa bwino wazoti mukambirane ndi malipoti azomwe zachitika.

Kuphatikiza pa misonkhano ya mamembala, mungafunenso kukumana ndi gulu la atsogoleri (akulu ampingo ndi atumiki (dikoni)) kosachepera kamodzi pa mwezi kuti mukambirane zokhudza mpingo. Mukukumana kumeneku, muzipemphera limodzi ndi gulu lanu la atsogoleri. Limodzi, mukhoza kukambirana nkhani zampingo, kukonza dongosolo lammene mpingo ukulire.

Kuonjezera apo, ukuyenera kukumana ndi atsogoleri a m'mautumiki monga iwo amene amatsogolera maphunziro a Baibulo (sande sukulu), milaga, amayi,

[9] Pa zambiri zokhudza kudalitsa ma ukwati ndi kuikitsa maliro, onani Mutu 41: "Kuyendetsa Mwambo wa Ukwati ndi Maliro."

abambo, achinyamata, oyang'anira za utumwi, odzala mipingo, osodza, opembedzera ndi ena.[10]

KUPEREKA MWAMBO KWA MAMEMBALA OPULUPUDZA

Nthawi imakwana pamene kumakhala kofunikira kupereka mwambo kwa mamembala opulupudza. Kupereka mwambo kumeneku ndi kugwiritsa ntchito ulamuliro wa malembo umene mpingo uli ndi udindo. (Mateyu. 18:15-20; Luka 17:3; Yohane 20:23; 1 Akorinto. 5:1-5; Aefeso. 5:11; 1 Timoteyo. 5:19-20). Monga Mbusa wa mpingo, osamaopa kuchita udindo umenewu. Koma pamene, pakuyenerera kupereka mwambo, udzichita molimba mtima komanso mokhudzika mtima, podziwa kuti cholinga cha kupereka mwambo chiri m'magawo awiri, kuyeretsa mpingo (Mach. 5:9-11) ndi kubwezeretsa olakwa (Agal. 6:1).

Pamene inu ndi atsogoleri mwaona kuti mwambo ukuyenera kuperekedwa, mutsatire dongosolo limene anakhazikitsa Yesu mu Mateyu 18:15-20. Dongosolo limeneli liri ndi zigawo zitatu. Poyamba, abusa kapena atsogoleri a mpingo amene apatsidwa udindo umenewu apite kwa membala yemwe walakwila kukambirana zolakwitsa zake kapena milandu yake ndi kumudandaulira kuti alape. Ngati kuyesayesa uku sikuphula kanthu, ochimwayo ayitanidwe kuti akumane ndi abusa komanso akulu ampingo. Ngati membalayu wakana kulapa, nkhaniyi idziwitsidwe ku mamembala pa zokambirana za gulu lonse. Mamembala okhawo amene ndi ovomerezeka ndiamene amaloledwa kukhala nawo pa nkumano umenewu. Chimene mpingo ugwirizane apa chidzakhala chiganizo chomaliza. Ngati apezeke olakwa, umembala wake udzathetsedwa ndipo adzadulidwa kumpingo (Mateyu. 18:17). Komabe, nthawi zina, chilango chochepera chimatha kukhala choyenelera.

[10] Pa zambiri zakumvetsetsa za kugwira ntchito ndi atsogoleri a utumiki, onani mutu 33: "Kusokhanitsa Atsogoleri omwe si Abusa" ndi mutu 34: "Kutsogolera Nthambi za Mpingo."

~ Gawo 9 ~

MBUSA WA CHIPENTEKOSTE PA UTUMWI

~ Mutu 36 ~

Kumvetsetsa Kachitidwe ka Zinthu M’chipangano Chatsopano

Baibulo limatiuza nkhani yokondweretsa ya cholinga chopitilira cha Mulungu yowombola mtundu otayika wa anthu. Limapitiliranso kutiuza mmene amamemezera onse omtsatira iye kuti agwire nawo nchitoyi. Potero, Mbusa aliyense wa Chipentekoste adzipereke yekha kuntchito yofunikirayi. Tizidzifunsa tokha, “ndingatsogolere bwanji mpingo wanga kutengapo gawo lake pakukwaniritsa ntchito ya Mulungu kwathu, mu Afirika ndi kufikira dziko lonse lapansi.” Yankho lake ndi lakuti titsatire chitsanzo cha utumiki chimene Yesu ndi atumwi anakhazikitsa.

Kudzera m’moyo ndi utumiki wake, Yesu anaonetsera chitsanzo chokhazikika bwino chammene mpingo ungachitire ntchito ya utumwi. Atumwi anamvetsetsa izi, ndipo anatsanzira chitsanzo cha Yesu. Monga abusa a Chipentekoste, ndi olowa mmalo mwa Khristu pantchito yake, tikuyenera kuchita chimodzimodzi. Chitsanzo chimenechi nthawi zina chimatchedwa “Njira za Mzimu Mchipangano Chatsopano.” Mutu uno uwunguza mosamala bwino lomwe njira zimenezi. Uperekanso maganizo ake pa mmene inu mungagwiritsire ntchito njirazi pa mpingo wanu monga Mbusa wa Chipentekoste ku Afirika.

CHOLINGA CHA UTUMWI WAM'BUKU LA MACHITIDWE

Luka analemba buku la Machitidwe ndi cholinga choonetsera kachitidwe ka utumwi. Analemba kuyitanira mpingo wa munthawi yake komanso mpingo mzaka zonse zilinkudza kuti ubwerere kutsatira mizu yake ya Chipentekoste ndi utumwi. Pofotokozera owerenga ake pazammene mpingo unayambira ndi mmene mpingo unapambanira mumphamvu ya Mzimu angakhale pakatikati pa mazunzo ochuluka, Luka amafuna kulimbikitsa mpingo kuti uchite chimodzimodzi. Potero, Luka analemba buku la Machitidwe kuti awonetsere kachitidwe ka utumwi kamene kangapambane muchikhalidwe chamtundu uliwonse wa anthu komanso munthawi ndi nyengo zosiyanasiyana mpakana Yesu atadza.

Cholinga chenicheni chimene Luka analembera bukuli chikuululidwa mu Machitidwe 1:8 pamene Yesu anaauza ophunzira ake kuti, "Komatu mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya monse, ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko." Mawu awa a Yesu ndi chifungulo pakumvetsetsa kachitidwe ka utumwi kamene kaonetseredwa mumachitidwe. Kakuwonetsera ndondomeko imene yabwerezedwa m'buku lonse la:

Kupatsidwa Mphamvu ndi Mzimu Woyera
— Nthawi zonse kumatsatidwa ndi—
Kuchitira umboni mwa Mphamvu ya Mzimu.

Machitidwe a mtundu uwu muzolemba za Luka amaonetsa chikhalidwe chopatsidwa mphamvu zochitira umboni. Mu buku la Machitidwe, kachitidwe aka ndi kobwerezedwabwerezedwa. Nthawi zonse Mzimu akatsanulidwa, zotsatira zake ndi kuchitira umboni mwamphamvu ya Mzimu. Palibe machitidwe a mtundu wina.[1]

Lonjezano la Machitidwe 1:8 likutikhudzabe ife lero lino. Monga ophunzira oyamba aja, ifenso tikhoza kulandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa ife. Ndipo monga iwo, tikhoza kukhala Mboni za Khristu mumphamvu ya Mzimu kwathu komanso kufikira kumalekezero adziko.

[1] Kuti mupeze zambiri pankhaniyi, onani mabuku a Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Machitidwe: Mzimu wa Mulungu mu Utumwi,* lolembedwa ndi Denzil R. Miller.

NJIRA YA CHIPANGANO CHATSOPANO

Tiyeni tione momwe Paulo anagwiritsira ntchito njirayi munzinda wa Chiroma wa Aefeso (Mach. 19:1-11). Pochita ichi, tidzazindikira kuti njira ya Paulo inali ndendende njira imene Yesu anagwiritsira ntchito pakumemeza mpingo wake kuti uchite usodzi, kudzala mipingo ndi utumwi.

Utumiki wa Chitsanzo ku Aefeso

Pakufotokozera nkhani ya utumiki wa Paulo ku Aefeso, Luka akuonetsera chitsanzo chokwanira bwino cha njira imene Paulo anagwiritsa ntchito ku Aefeso mu utumiki wake. Zimayenera kukhala njira yoti igwiritsidwe ntchito masiku onse mumpingo pakudzala mipingo. Tiyeni tione mmene Paulo anachitira pogwiritsa ntchito njira ya Mzimuyi mu utumwi wake podzala mipingo, osati ku Aefeso kokha, komanso ku Asia konse.

Kutsanulidwa kwa Mzimu ku Aefeso (Machitidwe 19:1-7)

Paulo anafika ku Aefeso ndi cholinga chodziwika bwino mmalingaliro mwake. Cholingachi chikuululidwa mu ndime 10, pamene Luka akutiuza ife kuti patangotha zaka ziwiri zokha "Onse akukhala m'Asia anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene." Cholinga cha Paulo chinali kufikira Aefeso ndi onse aku Asia ndi uthenga wa Khristu. Paulo anali ndi njira yokwaniritsira izi yodziwika bwino m'malingaliro mwake. Njira iyi ikuwoneka poyera pakuunguza mozama utumiki wake ku Aefeso opezeka mu Machitidwe 19:1-11. Ndi ichi mmalingaliro, tiyeni tione chimene Paulo anachita ku Aefeso.

Pamene Paulo anafika mu mzinda, anapeza ophunzira khumi ndi awiri. Amuna amenewa akuyenera kuti anali atsogoleri mumpingo omwe umangotumphuka kumene ku Aefeso (Mach. 18:24-27). Nthawi yomweyo Paulo anawafunsa iwo, "Kodi munalandira Mzimu Woyera pomwe munakhulupirira?" (19:2). Mtumwi anafunsa funso limeneli kuti azindikire ngati anthu amenewa anali okonzekeretsedwa ku uzimu kuti agwire nawo ntchito ya utumwi kufikira Aefeso ndi Asia yense ndi uthenga wabwino. Iye amagwiritsa ntchitochiphunzitso cha Yesu mu Machitidwe 1:4-8 (onani Luka 24:49).

Atatha kukambirana mwachidule, Paulo anaika manja pa okhulupirira khumi ndi awiriwo ndipo " Mzimu Woyera anadza pa iwo; ndipo analankhula, ndi malilime, nanenera" (Mach. 19:6). Nusu yakuti, "Mzimu Woyera anadza pa iwo" itikumbutsa ife lonjezano mu Machitidwe 1:8, pamene Yesu anati, "Komatu

mudzalandira mphamvu, *Mzimu Woyera atadza pa inu:* ndipo mudzakhala mboni zanga" (kutsimikiza kwachita kuwonjezeredwa). Kuunikira uku kukhoza kutithandizira ife kuti timvetse zimene zimachitika mu ndime imeneyi. Mzimu Woyera "anadza pa" iwo monga mmene anabwelera pa ophunzira pa Tsiku la Pentekoste kuti awapatse mphamvu kukhala mboni mu Yerusalemu, ndi mu Yudeya ndi mu Samariya, ndi kumalekezero adziko lapansi."

Pamene Mzimu anadza pa khumiwo ku Aefeso, "analankhula, ndi malilime, nanenera," pamenepo anaonetsera kuti Khristu wa wapatsa mphamvu kuti ayankhule m'malo mwake.

Makopedwe Ku Aefeso (Machitidwe 19:8-11)

Pamene amuna khumi ndi awiriwa anapatsidwa mphamvu, ndi Mzimu Woyera, Paulo anakhazikitsa ntchito yolalikira kwa otayika ndi kudzala mipingo imene inapitilira kwa zaka ziwiri ndipo zotsatira zake "onse akukhala m'Asia anamva mau a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene" (v. 10). Chokwaniritsa chotani ichi! Mu zaka ziwiri zokha, aliyense wa ku Asia-angakhale enanso a mitundu ina yosiyanasiyana ndi mafuko ena anamva uthenga wabwino. Kuphatikiza apo, mipingo yambiri inadzalidwa. Chiwerengero chimenechi chiyenera kuphatikizapo mipingo isanu ndi iwiri yonenedwa mu Chivumbulutso 2-3.

Njira ya Mzimu

Luka anaphatikizapo nkhani ya utumiki wa Paulo ku Aefeso monga chitsanzo chake chokwanira bwino cha ndondomeko ya utumwi wa Mtumwi. Ndipo zenizeni zake ndi zakuti ikuphera mphongo ndondomeko yake ya utumwi yomwe inawonetseredwa mu ulendo wake oyamba ndi wachiwiri wa utumwi. Ndi ndondomeko imene ife ngati abusa a Chipentekoste tikuyenera kugwiritsa ntchito mu usodzi ndi kudzala mipingo lero. Tiyeni tiunikire bwinondondomeko ya Mzimuyi. Ndondomeko ya Paulo ikuphatikiza nsanamira zitatu motere:

1. Nsanamira yoyamba: Kupereka mphamvu. Mzati kapena nsanamira yoyamba ya kachitidwe ka utumwi ka Paulo kanali kupereka mphamvu. Kupereka mphamvu kunali m'magawo awiri. Poyamba, kumakhudza kupereka mphamvu kwa *mtumwiyo*. Komanso kupereka mphamvu kumakhudza *mpingo*, kapena mipingo imene ikudzalidwa. Tiyeni tiwone chimodzi-chimodzi cha zinthu zofunikirazi:

Paulo anafika kwa Aefeso odzala ndi Mzimu Woyera. Kumeneko anatumikira monga mboni yopatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera monga m'mene Yesu anafotokozera mu Machitdwe 1:8. Chokha chongoti anatha kuwasanjika manja ophunzira khumiwa ndi kuwalimbikitsa kuti adzazidwe ndi Mzimu Woyera zikuonetseratu kuti iye mwini wake analinso odzazidwa ndi Mzimu. Kuonjezera apo, mbuku lonse la Machitidwe, Luka akupereka zitsanzo zochuluka za utumiki wa mphamvu ya Mzimu wa Paulo (Monga., Machitidwe 9:17-20; 13:4-5, 9-11; 14:8-10; 15:12).

Komabe, zikuoneka kuti Paulo, anazindikira kuti sizinali zokwanira kuti iye yekha ndiamene akhale odzazidwa ndi Mzimu. Anadziwa kuti, ngati ntchitoyi ingapite patsogolo, ndiye kuti nawonso mpingo wa ku Aefeso upatsidwe mphamvu ya Mzimu Woyera. Potero, pamene anafika mu mzindawo, ntchito yoyambirira ya Paulo inali kuonetsetsa kuti okhulupirira onse mu mzindawu abatizidwa ndi Mzimu Woyera. Nchifukwa chake anawafunsa ophunzira khumiwo, "Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?" Ndipo ndi chifukwa chake anawapempherera msangamsanga kuti alandire Mzimu. Pamenepa, zinthu ziwiri zofunika za nsanamira yoyamba ya kachitidwe ka utumwi ka Paulo ndi kupereka mphamvu kwa ochita utumwi, komanso ku mpingo.

Pamenepo atatha kupatsidwa mphamvu, mpingo waku Aefeso unakhala chikatikati cha machitachita a utumwi ndikufikira ngodya iliyonse ya delaro. Zinthu ziwiri izi, kupatsidwa mphamvu kwa Mbusa ndi kupatsidwa mphamvu kwa mpingo, zikuyenera kukhala gawo la upangili wathu wa utumwi lero. Upangili wa Paulo wa Mzimu waonetseredwa muchithunzi chili munsichi:

"UPANGILI WA MZIMU" WA MCHIPANGANO CHATSOPANO
(Machitidwe 19:1-11)

Nsanamira 1: Kupereka Mphamvu:

► *Kwa mtumwi*

► *Kwa mpingo*

Nsanamira 2: Kukhala Mboni:
- ► *Kulalikira*
- ► *Kuwonetsera*

Nsanamira 3: Kumemeza Anthu:
- ► *Kuphunzitsa*
- ► *Kutumiza*

---

2. Nsanamira Yachiwiri: Mboni. Nsanamira yachiwiri ya upangili kapena kachitidwe ka utumwi ka Paulo ndiyo kukhala mboni. Izi kukuyenera kuyembekezeka popeza kuchitira umboni molimba mtima ndicho chiyembekezero cha kudzazidwa ndi Mzimu Woyera (Mach. 1:8; 4:31). Monga ndi kupatsidwa mphamvu, umboni uli ndi zigawo ziwiri: Kulalika ndi kuonetsera (onani chinthunzi 1).

Choyamba, Paulo anachitira umboni kudzera mukulalika kwamphamvu kwa uthenga wabwino. Kulalikaku kunayamba pamene ophunzira khumi ndi awiri aja "anayankhula malilime ndi kunenera." Pogwiritsa ntchito Machitidwe 1:8 monga chifungulo chathu potanthauzira, tikuzindikira kuti kunenera kwawo kunali kudzera mukulalika uthenga wabwino kwamphamvu ya Mzimu kwa otayika, monga m'mene Petro analalikira mwa uneneri pa Tsiku la Pentekoste (2:4).

Luka, kenako akutiuza kuti Paulo "analowa m'sunagoge, nanena molimba mtima, miyezi itatu, natsutsana ndi kukopa za Ufumu wa Mulungu" (Machitidwe 19:8). M'buku la Machitidwe, kulalika Ufumu wa Mulungu ndi chimodzimodzi kulalika uthenga wabwino wa Khristu (8:12; 28:23, 31). Kuonjezera pa kulalika Khristu m'masunagoge, Paulo "anaphunzitsa….pabwalo ndi m'nyumba zanu ndi kuchitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuka mtima kulinga kwa Mulungu, ndi chikhulupiriro cholinga kwa Ambuye wathu Yesu Khristu" (20:20-21). Umboni wapakamwa wa Paulo ku Aefeso unatsagana ndi chionetsero cha mphamvu ya ufumu kudzera mu zizindikiro zotsatira (19:11-20).

Chomwecho, monga zinaliri ndi nsanamira yoyamba, nsanamira ya chiwiriyinso ya upangili wa utumwi wa Paulo inali ndi zigawo ziwiri, kulalika mwa mphamvu ndi chionetsero cha mphamvu ya mu ufumu kudzera m'zizindikiro

zotsatira. Ndizosakaikitsa kuti utumiki wa anzake a Paulo omwe anali atangodzazidwa ndi Mzimu kwatsopano unaphatikizapo zinthu ziwiri zimenezi, kulalika ndi kuonetsera.Zinthu ziwiri izi zikuyenera kukhala ndi mboni iliyonse ya Chipentekoste mu Afirika lero.

3. Nsanamira Yachitatu: Kumemeza. Nsanamira yachitatu ya upangili wa utumwi wa Paulo wa Mzimu unali kumemeza. Pamene mpingo unangopatsidwa mphamvu ndi Mzimu—ndipo uthenga umalalikidwa—Paulo anayamba kumemeza mpingo ku utumwi wa m'madera. Kumemeza uku kwatchulidwa m'Machitidwe 19:10: "Ndipo anachita chomwechi zaka ziwiri; kotero kuti onse akukhala m'Asiya anamva mawu a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene." Osachoka m'Aefeso, Paulo anakwanitsa kufikira dera lonse la Asiya ndi uthenga wabwino muzaka zochepa chabe ziwiri. Izi zikanatha kukwaniritsidwa pochita zothekera kumemeza ophunzira mu Aefeso.

Malembowa akunena kuti Paulo anamemeza mpingo wa ku Aefeso munjira ziwiri, kuphunzitsa ndi kutumiza (onani chithunzi 1). Poyamba, Paulo *anaphunzitsa* ogwira ntchito ndi odzala mipingo ku sukulu ya Turano (Machitidwe 19:9). Kalembedwe ka mawuwa kakuonetsera ubale ochita ndi kuchititsa pakati pa maphunziro a utsogoleri a Paulo ndi nkhani yakuti aliyense okhala m'Asiya anamva mawu a Ambuye mzaka ziwiri zokha. Dongosolo la zophunzitsidwa kusukuluyi likuyenera kuti linaphatikizirapo kutsindika kwa mphamvu pa usodzi ndi kudzala mipingo. Kuphatikiza apo, zochitika za pasukulupo zikuyenera kuti zinali zosefukira ndikupezeka kwa Mzimu.

Kaphunzitsidwe ka Paulo kakuoneka kuti kamaphatikizirapo kuphunzitsa munthu pogwira ntchitoyo ndikumamuthandiza m'mene ayenera kuchitira. Izi zakhudzidwapo mu Machitidwe 19:8-9, pamene Paulo akuphatikizapo ophunzira ongodzazidwa kumene ndi Mzimu mu utumiki wake wa usodzi. Ubale wothandizara ophunzirawu ukupitilira kuonekera m'mene iye anakhalirabe chifupi ndi ophunzirawa ku Aefeso (v. 9; 20:1, 17-18). Paulo akuyenera kuti anaphunzitsa ophunzirawa munjira zomwe iye amachitira utumwi wake. Analemba kwa Timoteo nthawi ina patsogolo kumulangiza iye, "Ndipo zimene iwe wazimva kwa ine mwa mboni zambiri,zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsanso enanso" (2 Tim. 2:2).

Pamene ophunzirawa anadzazidwa ndi Mzimu ndi kuphunzitsidwa, kapenanso adakachitabe maphunzirowo, Paulo anawatumiza kungodya zonse za m'derali kuti akalalikire uthenga ndi kudzala mipingo yopatsidwa mphamvu ndi

Mzimu. Mosakayikila, nawonso anagwiritsa upangili wa utumwi omwewo umene amagwiritsa ntchito mphunzintsi wawo. Kugwiritsa ntchito kwa upangili umenewu kunatsatira mu kutumphuka kwa mipingo yodzalidwa m'dera lonse (Mach. 19:10). Ndizoonekeratunso poyera kuti upangili wa Paulo unaphatikizirapo kufikira anthu a mitundu ndi zikhalidwe zosiyanasiyana, pakuti Luka akuti "Ayuda ndi Ahelene omwe" analalikidwa uthenga wabwino.

Chitsanzo cha Yesu

Ndikofunikira kudziwa kuti Paulo sanali oyambitsa upangili omwe anagwiritsa ntchito ku Aefeso ndi Asia. Iye amangotsatira chitsanzo cha Yesu pamene anatumiza mpingo wake kudziko lapansi.

Yesu anamemeza ophunzira ake pa *kuwaphunzitsa* ndi kuwatumiza iwo kuti amuke (Marko 3:13-15). Pamene iwo amapita, amayenera *kulalikira* uthenga ndi *kuonetsera* mphamvu ndi zizindikilo zotsatira (Marko 16:15-18). Asanachite ntchito ina iliyonse, anayenera kudikira m'Yerusalemu kuti *apatsidwe mphamvu* ndi Mzimu (Luka 24:49; Machitidwe 1:4-8) monga m'mene Yesu mwiniwake anapatsidwira mphamvu ndi Mzimu (Luka 4:18-19; Mach. 10:38). Kupatsidwa mphamvu kwa ophunzira kunachitika pa Tsiku la Pentekoste ndi panthawi zina zambiri m'Machitidwe. Paulo mukukopa kwake kwa anthu aku Aefeso amatsatira chitsanzo cha Yesu potumiza mpingo wake kudziko lonse.

MAPHUNZIRO A LERO

Monga abusa a Chipentekoste, tingathe kuphunzira maphunziro ofunikira kuchokera mu kafukufuku wa utumiki wa Paulo opatsidwa mphamvu ndi Mzimu ku Aefeso. Tiyeni tiwone maphunziro atatu amenewa:

Landira Mphamvu ya Mzimu

Poyamba tikuphunzira kuti tisamaganizire kugwira ntchito ya Mulungu mu mphamvu ndi kuthekera kwathu. Kumbali inayi, monga Yesu ndi Paulo, tikuyenera kutumikira mumphamvu ndi kudzoza kwa Mzimu. Kolingana ndi chitsanzo cham'buku la Machitidwe, mphamvu za umulungu zimadza pamene tabatizidwa ndi Mzimu wa Mulungu ndi kupatsidwa mphamvu ndi Mzimu wa Mulungu. Zimakhalabe pamene tiyenda mu Mzimu.

Tikupitilira kuphunzira kuti ngati mipingo yathu ingakhale chikatikati cha machitachita opindulitsa a usodzi, kudzala mipingo, ndi utumwi, ikuyenera

kukhala ndi umoyo oyenera wa uzimu mkati mwake opangitsa kuti cholinga chimenechhi chitheke. Potero, monga abusa a Chipentekoste, ntchito yathu yoyambirira ikhale kuonetsetsa kuti mipingo yathu yadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Tikhoza kufikira cholinga ichi pakuonetsetsa kuti iwo onse amene abwera kwa Khristu atsogoleredwa kukulandira ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kuphunzitsidwa m'mene angakhalire odzazidwa ndi Mzimu. Kuphatikiza apo, tiwatsogolere anthuwa kukhala mboni zodzidwa ndi mphamvu ya Mzimu.[2]

Gwiritsani Ntchito Upangiri wa M'Baibulo

Chachiwiri, tikuphunzira kufunikira kogwiritsa ntchito upangiri wa m'Baibulo, otsogozedwa ndi Mzimu pogwira ntchito ya usodzi, kudzala mipingo ndi utumwi. Ku Aefeso, Paulo anatsogozedwa ndi upangili oterewu. Unali upangili okhazikika pa chitsogozo cha umulungu osati nzeru za umunthu. Paulo amatsatira chabe upangili kapena njira zimene Yesu anagwiritsa ntchito pomemeza mpingo wake ku utumwi wa dziko lonse.

Kuonjezera apo, Paulo analinga kukafalitsa mipingo ya utumwi yodzazidwa ndi Mzimu Woyera ku Asia konse. Uliwonse mwa mipingoyi imakhala mwa iyo yokha masomphenya ndikuthekera kwa uzimu kumene kumasowekera kuti akabzale mipingo ina ya utumwi yodzazidwa ndi Mzimu. Mwanjira iyi, mipingo inachulukitsidwa ku Asia konse, ndipo uthenga wabwino unalalikidwa ndi mphamvu kwa onse akukhala komweko—Ayuda ndi Ahelene.

Lero, ife monga abusa a Chipentekoste tichite chimodzimodzi. Zoonadi, tikuyenera kukangalika kupulumutsa anthu. Komabe,tikuyenera kuzindikra kuti usodzi, angakhale kuti ndi ofunikirachonchi, si okwanira paokha. Tidzale ndi kukuza mipingo ya utumwi yodzazidwa ndi Mzimu-mipingo imene anthu ongotembenuka mtima kumene adzazidwa ndi Mzimu, aphunzitsidwa ndi Mzimu munjira za Khristu, owumbidwa kuti akachitechite popititsa ufumu wa Mulungu patsogolo, ndikumemezedwa ndi kutumidwa kuti akachite chimodzimodzi m'madera oyandikira ndi akutali komwe.

---

[2] Kuti mudziwe zambiri pakulimbikitsa mpingo kufuna Mzimu, onani Mutu 19: "Kutsogolera Mpingo ku Chitsitsimutso cha Chipentekosite." Kuti mudziwe zambiri pa kutsogolera ophunzira kupatsidwa mphamvu ya Mzimu, onani mutu 20: "Kutsogolera Okhulupirira mu Ubatizo wa Mzimu."

Yendani ndi Cholinga

Pomaliza, muzonse zomwe tichita tikuyenera kuyenda mwadaladala ndi cholinga. Zochitika zambiririmbiri za pampingo zimachitika popanda cholinga chenicheni. Zambiri, timangoyerekezera. Sitingangoyerekezera kuti anthu adzabwera ku mpingo wathu chifukwa choti tatsekula zitseko la Mulungu lililonse. Sitingangoyerekezera kuti anthu akubadwa kwatsopano chifukwa chakuti tikuwatsogolera mu "pemphero la kulapa." Sitingangoyerekezera kuti okhulupirira akudzazidwadi ndi Mzimu kutengera pa machitachita a Mzimu owonekera kunja kwa thupi. Sitingangoyerekezera kuti mpingo umene tikuubusa ndi wodzazidwa ndi Mzimu chifukwa ulim'banja la Chipentekoste kapena Chikarazimatiki. Sitingangoyerekezera kuti mpingo wathu ukhala ndi masomphenya ndi changu cha utumwi chifukwa mpingowu umakhulupirira zimenezi. Kumbali inayi, tikhale ndi lingaliro lodekha bwino lazomwe tikufuna tikwaniritse, ndipo tidziwe m'mene tichitire kuti tikwaniritse zolinga zathu.

M'chitidwe wadaladala udzioneka pa chiganizo ndi pa china chilichonse chimene tikufuna tichite. Tikuyenera tifunefune nkhope ya Mulungu ndi cholinga choti tidzazidwe zenizeni (kapena kudzazidwanso) ndi Mzimu Woyera. Tikuyenera kulalikira uthenga ndi cholinga chowona miyoyo yotayika ikulapa ndi kubadwadi kwatsopano. Tipemphere ndi okhulupirira ndi cholinga choti adzazidwedi ndi mphamvu ya Mzimu wa Mulungu. Tidzale mipingo ndi cholinga chowerengeratu kuti ikhale mipingo ya utumwi yodzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu..

Nthawi zonse, mwadaladala tidzipereka masomphenya athu ndi upangiri wathu ku atsogoleri amene Mulungu wawadzutsa mu mpingo. Pamenepo timemeze mpingo ndi chindunji chadaladala chofikira mzinda, dziko, dera ndi mafuko ndi uthenga wabwino. Izi ndi zimene Yesu anachita, ndipo ndi m'mene Paulo anafikila Asiya yense ndi uthenga wabwino muzaka ziwiri zokha. Izi ndi zimene tikuyenera kuchita lero.

~ Mutu 37 ~

Kulalikira Otayika

Ndizofunika bwanji kutsogolera angakhale munthu m’modzi kwa Khristu? Inde, kwa munthuyo ndichofunikira kwa muyaya. Komabe, machitidwe awa a chikondi chachi Khristu akhoza kukhala ofunikira kwa muyaya kwa anthu enanso ochuluka monga m’mene nkhani ili m’musiyi ikufotokozera.

Edward Kimball anali munthu wamba ogulitsa mu sitolo kuDetroit, Michigan, USA. Analinso mphunzitsi wa Sande Sukulu ku mpingo wake. M’chaka cha 1854 anakumana ndi mnyamata wa zaka khumi kudza mpambu zisanu ndi ziwiri (17) otchedwa Dwight ndipo anamutsogolera kwa Khristu. Mnyamatayu anakula ndikukhala mlaliki odziwika kwambiri, Mlaliki D. L. Moody. Moody anakhala m'modzi mwa azilaliki amene anabweretsa miyoyo yochuluka kwambiri mumbiri ya utumiki. Moody anapangitsa F. B. Meyer kulowa mu utumiki wakulalikira kwa otayika ndi utumwi, ndipo iyenso anapangitsa J. Wilbur Chapman, amenenso anaphunzitsa Billy Sunday kukhala mlaliki. Aliyense amene anaphunzirako mbiri ya mpingo amadziwa kuti amuna onsewa sanali anthu wamba, zinali ziphona, azilaliki amphamvu. Limodzi anapindula miyoyo yochuluka kwa Khristu. Koma nkhaniyo sikuthera pompo.

Mlaliki oyenda yenda otchedwa Mordecai Ham anatakasidwa ndi utumiki wa Billy Sunday. Kenako mu chaka cha 1934, Ham analalikira uthenga umene unasuntha Billy Graham kuti apereke moyo wake kwa Yesu. Billy Graham ndi munthu amene analalikira uthenga wabwino kwa anthu ochuluka kuposa munthu

wina aliyense mumbiri. Tangolingalirani, zonse izi zikutsatira chimene mphunzitsi wa Sande sukulu uja anachita polalikira kwa mnyamata pa nseu. Nkhani ya Edward Kimball ikuonetsera mmene kulili kofunikira kwa Mbusa wa Chipentekoste kuti atsogolere mpingo wake kukachita usodzi wamphamvu. Mutu uno ofotokoza zam'mene tingachitire izi.

MATANTHAUZO

Monga Mbusa wa Chipentekoste, ukuyenera kukhala ndi kumvetsetsa kopanda ziyangoyango kuti kulalikira kwa otayika kapena kuti usodzi ndi chiyani ndikuti zikukhudzana bwanji ndikudzala mipingo ndi utumwi. Pamene zinthu zitatu zonsenzi zikuchokera ku Kutuma Kwakukulu (Mateyu. 28:18-20; Marko 16:15-16), pali kusiyana kofunika kukudziwa.

Usodzi/kulalikira kwa otayika

Usodzi ndi kugawana uthenga ndi anthu otayika ndicholinga chowakopa kuti abwere kwa Khristu. Kumakhudza kuwauza anthu za Yesu ndi ntchito yake yopulumutsa ya pa mtanda ndi kuwayitana kuchikhulupiriro cha mwa Iye (Mach. 16:31). Pamtima pa usodzi ndi nkhani ya Imfa ndi Chiukitso cha Yesu (1 Ako. 15:1-4). Usodzi ukuposera ndondomeko ya pa mpingo, usodzi ndiye cholinga chimene mpingo udakhazikitsidwira. Usodzi ndi udindo wapaderadera wa Mkhristu wina aliyense.

Kudzala mpingo

Kudzala mpingo kumakhudzanso kulalikira kwa otayika, koma kumafuna zinthu zochuluka. Kudzala mpingo kumafuna dongosolo kwaiwo amene atembenuka mtima kuti adzikumana monga thupi la okhulupirira. Okhulupirirawa amakumana pafupipafupi mchiyanjano, pemphero ndi kuphunzira Baibulo. Atsogoleriamasankhidwa kuti aphunzitse okhulupirirawa, kuti aumbike kukhala m'chifaniziro cha Khristu. Okhulupirira atsopanowaamaphunzitsidwa kusiya njira zawo zauchimo zakale, ndikukhala kolingana ndi mawu a Mulungu, ndikuuza ena za Yesu.

Utumwi

Utumwi umaphatikiza zonse; usodzi ndi kudzala mpingo. Komabe pali kusiyana kozindikirika ndithu. Utumwi umakhudza kupindula miyoyo yotayika

kwa Khristu ndi kudzala mipingo mzikhalidwe zosiyana. Zimafunikira kuti ochita utumwi achoke mmakomo mwawo ndikupita kumalo atsopano, kuphunzira chiyankhulo chatsopano ndikudzizoloweletsa moyo ndi chikhalidwe chakumalo atsopanowo. M'malo achilendowa amapindula miyoyo kwa Yesu ndi kuyambitsa mipingo yatsopano.

Paulo ndi chitsanzo cha mtumwi. Anapita kumalo, kuwoloka malire kukalalika Khristu kwa otayika. Pamene amachita izi, amadzala mipingo ndi kuyang'anira mmene ikukulira. Pofuna kuwonetsetsa kuti mipingoyi ikukula, Paulo amasankha atsogoleri ndi azibusa kuti atsogolere mipingoyi. Wina mwa udindo wa abusa unali kutsogolera mipingo yawo kulalikira kwa otayikandikutumizanso atumwi kuchoka pakati pawo. Izi zimapangitsa kuti ntchito ya usodzi, kudzala mipingo ndi utumwi zipitirirebe (onani 1 Atesalonika 1:8).

UDINDO WA UBUSA

Paulo analemba kwa Timoteo, mwana wake m'chikhulupiriro komanso Mbusa wa mpingo waku Aefeso, kumuuza iye kuti "chita ntchito ya mlaliki wa Uthenga Wabwino" (2 Timoteo 4:5). Ntchito ya mlaliki ndiyo kupindula miyoyo kwa Khristu ndi kuphunzitsa ena kuti achite chomwecho (Aef. 4:11-12). Monga Mbusa wa Chipentekoste, iwenso wasenza udindo womwewu. Ukonze dongosolo lomemeza mpingo wako kukachita usodzi wa mphamvu. Dongosolo la kumemeza uku liphatikizepo zinthu zitatu izi:kulimbikitsa, kuphunzitsa ndi kutumiza motere:

Kulimbikitsa

Monga Mbusa wa Chipentekoste, ntchito yanu yoyamba posonkhanitsa mpingo ku usodzi ndi kuikiza m'mitima ya anthu a Mulungu chikondi pa otayika. Njira imodzi imene mungachitire izi ndiyo kuwaphunzitsa iwo chimene Baibulo limanena pa zakutayika kwa munthu. Kupatulapo kukhala paubwenzi opulumutsa ndi Yesu Khristu, anthu onse alibe chiyembekezo ndipo atayika kwa muyaya. Chiyembekezo chawo chokhacho m'moyo uno ndi omwe ulinkudza ndi kumudziwa Yesu. Ukuyenera kuikiza choonadi chodabwitsa ichi m'mitima ndi m'malingaliro awo. Kuwonjezera apo, muwakumbutsenso za udindo wawo ogawana ndi otayika.

Kuti mukwaniritse izi, mukusowekera kudalira Mzimu wautumwi wa Mulungu. Mudziwonetsetsa kuti mamembala anu adzazidwa ndi Mzimu Woyera

ndi mphamvu monga mboni za Khristu (Machitidwe 1:8). Muyenera kuonetsetsa kuti kupezeka ndi mphamvu ya Mzimu kumaonekera mu mwambo wanu wa mapemphero. Ngati mutampatsa mpata, Mzimu Woyera adzayenda m'mitima ya anthu kuwaumba ndi kuwalozera ku kholola.

Kuphunzitsa

Njira ina imene mungamemezere anthu mumpingo ku usodzi ndiyo kuwaphunzitsa. Izi ndi zimene Yesu anachita. Anawalangiza ophunzira ake, "Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu" (Marko 1:17). Pamene ophunzira a Yesu amatsatira Mbuye wawo, kumvetsera chiphunzitso chake, ndi kutsanzira njira zake, anasanduka ziphona zolalika uthenga wabwino.

Machitachita omwewa akuyenera adzichitika m'mipingo yathu ya Chipentekoste lero. Tidziwaphunzitsa ma membala athu m'mene angasodzere miyoyo yotayika monga momwe anachitira Yesu ndi atumwi. Pochita ichi, tidziwaphunzitsa m'mene angayendere muuzimu ndi kuzindikira liwu la Mzimu Woyera pameneakuwatsogolera iwo kuchitira umboni (fanizila Machitidwe 8:29). Monga abusa a Chipentekoste, tikuyenera kuphunzitsanso anthu athu m'mene angadziperekere ku kudzoza kwa Mzimu Woyera, kumudalira iye kuti ayankhule kudzera mwa iwo pamene akuwauza ena za Khristu.

Kuphatikiza apo, tionetsetse kuti oyera mtima akumvetsetsa ndipo akukwanitsa kulumikizana momveka bwino ndi ena. Adzizindikiranso mmene angatsogolere anthu kwa Yesu, kuwamema kukulapa ndi chikhulupiriro. Njira imodzi tingakwaniritsire izi ndi pokonza misonkhano ya pachaka pa usodzi opatsidwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

Kutumiza

Pamene anthu a Mulungu alimbikitsidwa ndi kuphunzitsidwa, akuyenera kutumizidwa. Izi ndizimene Yesu anachita monga gawo la dongosolo la maphunziro ake, anatumiza ophunzira kukalalikira uthenga wabwino. Ndipo anabweretsa lipoti la mmene ayendera kuti iye awunikire momwe achitira (fanizila Luka 9:6; 10:1-20). Kenako, pamene utumiki wake pano pa dziko lapansi umalowera kumapeto, anawatumiza ophunzira akewa kuti apite kukachitira umboni"mu Yerusalemu, mu Yudea monse, ndi mu Samaria, ndi kufikira malekezero ake a dziko lapansi" (Machitidwe 1:8). Monga Mbusa wa

Chipentekoste, mudzichita chimodzimodzi. Mupereke moyo wachitsanzo wa usodzi ku mamembala anu. Muwaphunzitse kenakano nkuwatumiza ku utumiki.

NJIRA ZOCHITIRA USODZI

Monga Mbusa okhulupirika wa Chipentekoste, musakhale opusa kuti mungokhala waulesi, kuyembekezera kuti anthu am'dera lanu adzabwera ku mpingo wanu. Kapena kuganiza kuti mamembala anu mwadzidzidzi adzakhala mboni ku anzawo ndi okhala nawo chifupi. Monga Mbusa, mukhazikitse njira ndi kuyika m'malo ndondomeko zokonzekeretsa mpingo kukachita utumwi wa mphamvu.

Mungathe kuchita izi pogwiritsa ntchito njira zosiyana-siyana zochitira usodzi. Chisankho chanjira chitengera ndi malo amene mukupitako, anthu amene mukufuna kuwafikira, komanso chitsogozo cha Mzimu Woyera. Nazi zina mwa njira zimene mungagwiritse ntchito kukasodza anthu.

Mwambo wa Mapemphero Pafupipafupi

Kufikira otayika chikhale chapamtima cha mwambo wathu wa mapemphero a la Mulungu. Nthawi zonse mudzikhala mukuganizira za anthu otayika mu mpingo wanu. Ndipo mudzilalika mokhulupirika uthenga wabwino kwa iwo. Monga Paulo, mudzikhala ofunitsitsa kulalikira "Yesu Khristu yekha ndi Iye wopachikidwa" basi (1 Ako. 2:1-2). Nzomvetsa chisoni kuti membala abweretse nzake ku mpingo kumene choonadi sichikulalikidwa. Uthenga uliwonse omwe mungalalikire muphatikizemo kufotokozera dongosolo la chipulumutso ndi kuyitanira anthu kwa Yesu.

Kulalikira Munthu M'modzi Payekha

Kuphatikizirapo pa kulalikira uthenga wabwino mu mwambo wathu wa mapemphero, mudzionetsetsa kuti mamembala anu akudziwa m'mene angagawanirane uthenga wabwino ndi iwo amene ali kunja kwa mpingo. Kutumikira kwa otayika kwa mtundu uwu,kumatchedwa kulalikira/kukopa m'modzimmodzi. Monga Mbusa, mungafune kulimbikitsa mitundu iyi yakalalikidwe yochitidwa ndi munthu payekha.

Kulalika khomo ndi khomo. Mukuchitira umboni koyenda khomo ndi khomo kukopa anthu kwa Yesu, mamembala amaphunzitsidwa ndi kutumizidwa apite khomo ndi khomo kuchitira umboni okopaanthu ndi kuwadziwitsa kukhudzidwa

kwa mpingo ndi moyo wawo. Adzipereke kupempherera zosowa zawo, ndipo akhale okonzeka kugawana nawo uthenga iwo amene awonetsa chidwi.

Kulalikira kwa abwenzi. Uwaphunzitsenso ndi kuwalimbikitsa ma membala kuti adzipempherera chipulumutso cha abwenzi awo. Amupemphe Mulungu kuti atsekule mitima ya abwenzi awo ndi kupereka mwawi kwa iwo kuti athe kugawana nawo uthenga wabwino. Mpingo ungathe kufuna kukhazikitsa tsiku lapaderadera pa chaka lotchedwa "tsiku la abwenzi" pamene ma membala adzilimbikitsidwa kuyitanira anzawo ku mpingo. Patsikuli, abwenzi onse adzapatsidwe ulemu wapaderadera. Kenakano ulalikire uthenga wa chipulumutso ndi kupereka mpata oti alandire Khristu ngati Mpulumutsi.

Kulalikira kudzera m'makhalidwe. Mukuyeneranso kuphunzitsa anthu kuti zenizeni zake ka kulalikira kwa otayika sizochitika kapena dongosolo, koma moyo umene mukukhala. Muyenerakuwalimbikitsa kuchitira umboni ndi miyoyo yawo komanso umboni wamoyo wawo. Akhale okonzeka kugwiritsa ntchito mwayi ogawana nawo uthenga ena pamene akukhala kudzera muzokumana nazo mmoyo tsiku ndi tsiku.

Misonkhano ya Ulaliki Yokopa Anthu

Misonkhano yolalikira kukopa anthu (nthawi zina imatchedwa misonkhano ya Chitsitsimutso) ndi njira ina yabwino yotsogoleraanthu kwa Khristu. Msonkhano wokopa otayikawo ukhoza kuyendetsedwa chonchi: Inu pamodzi ndi atsogoleri anu mukonza masiku a msonkhano ndipo panthawi yoyenera, yambani kulengezetsa kumpingo komanso m'dera lomwe kuchitikire msonkhanowo. Pamene nthawi yamsonkhano yayandikira, mpingo uyambe kupemphera mwakathithi kupempherera nsonkhanowo. Mamembala amalimbikitsidwa kuyitanira achibale, anzawo ndi oyandikana nawo ku misonkhanoyi. Monga Mbusa, uonetsetse kuti amene wamuyitana kudzatumikira ali ndi mtima pa otayika ndi kuthekera kolalikira uthenga wabwino. Muonetsetsenso kuti mlalikiyo alalike uthenga mokhulupilika mumwambo uliwonse ndikupereka mpata kwa anthu kuti apulumutsidwe.

Mapemphero a Pa bwalo

Mukhozanso kufuna kutengera msonkhano okopa anthu kukulapa m'makwalala. Mukhazikitse magulu olalikira ndikuwatumiza ku misika, ndi m'malo ena amene kumapezeka anthu ochuluka. Akapangitse misonkhano

yakanthawi kochepa komayamphamvu. Mapempherowo aphatikizepo kuyimba nyimbo kuti zikope anthu ochuluka, anthu kuperekera ma umboni achisomo cha Mulungu chakusintha kwa miyoyo yawo ndi uthenga wachidule kutsatidwa ndi kuyitanira kuti alandire Khristu.

Kugawa Uthenga Olembedwa (matrakiti)

Njira ina yotsimikizika yogawira uthenga wabwino ndiyo kudzera mukugawira anthu uthenga olembedwa. Mukhoza kukonza tsiku lotumiza anthu kumalo osankhika kukagawa uthengaolembedwa mtimabuku. Mabuku amene mugawe akhale osankhidwa bwino. Akhale okopa kuwawerenga komanso olembedwa bwino ndipo awonetsere dongosolo la Mulungu la chipulumutso. Akhale ndi nkhani yokhudza dzina la mpingo, malo, manambala a foni, komanso webusaiti ndi keyala ya imelo ngati ilipo.

Kupemphera Moyendayenda

Mapemphero poyendayenda akhoza kugwiritsidwa ntchito kuti titsekule malo atsopano okachitira umboni wa uthenga wabwino. Akhozanso kugwiritsidwa kupangitsa okhulupirira kuti akhudzike mtima kukafikira otayika m'deralo ndi Khristu. Mpingo ukhoza kusankha magulu a anthu awiriawiri kupita m'malo osankhika. Pamene akuchita izi, akhale akupempha Mzimu Woyera kuti ayende pa anthu okhala m'deralo, kutsekula mitima yawo kuti alandire uthenga wabwino. Akhozanso kumamenya nkhondo ya uzimu, kulimbana, kutsutsana ndi kumanga ziwanda zimene zagwira anthu mundende zaku uzimu ndi zakuthupi.

Pamene maguluwa akuyendayenda m'deralo akupemphera, akhale otseguka ku mwayi opemphera ndi anthu ndi kugawana nawo iwo uthenga wabwino. Kupemphera mukuyendayenda m'dera ndi njira yabwino yokonzekeretsa nthaka kukadzala mpingo watsopano.

Kufikira Anthu Kudzera M'njira Zofalitsira Mauthenga

Ngati mpingo wanu uli ndikuthekera muzachuma, mukhozanso kuganizirapo zogwiritsa ntchito njira zofikitsira mauthenga kwa anthu ochuluka pakamodzi kulalikira uthenga. Mwayi wa njira zofikira anthu ochulukazi ndi monga kulalikira pa wailesi komanso wailesi ya kanema. Intaneti, komanso kulumikizana kwa anthu pa makina a intaneti zikhoza kugwiritsidwa ntchito mwaukadaulo kufalitsa uthenga. Popanga dongosolo lofuna kufikira anthu moteromu, mulingalirepo kuti

ngati dongosolo lanu silikhala lachikokoka m'malo moti akopeke, zikhoza kuwachotsera chidwi pa mpingo.

Kudzala Mpingo

Kafukufuku waonetsa kuti kudzala mpingo ndiyo njira yamphamvu yofikira otayika ndi uthenga wabwino. Anthu ambiri amadzipereka kwa Khristu m'mipingo yatsopano kusiyana ndi mipingo yokhazikika yakalekale. Kudzera mukudzala mipingo, mpingo sumangokula muchiwerengero chokha, komanso umafalikira m'dera lonse.[1]

Njira Zina Zaukatswiri

Ukuyenera kukhala okonzeka kulandira njira zina zaukadaulo zofikira anthu otayika. Chofunikira kwambiri ndichakuti, monga Mbusa wa Chipentekoste, nthawi zonse, udzikhala otseguka ku chitsogozo cha Mzimu Oyera kulenga ndi kukonza dongosolo latsopano lofikira anthu.

MWAYI WOFIKIRA OTAYIKA

Paulo analimbikitsa a Khristu aku Aefeso kuti akhale "akuchita machawi" (Aef. 5:16). Pamene nyengo zikusintha, mipata yatsopano yofikira anthu otayika idzidzipezeketsa yokha. Monga Mbusa wa Chipentekoste, ukuyenera kutsogozedwa ndikukhala okonzeka kuyankhapo kuzosowa pamene zikudzuka. Tatengani zitsanzo zinayi izi za mwayi umene ungapezeke:

Kuvomera ku Mavuto

Mavuto amene amagwera anthu m'dera monga nkhondo, njala, milili, chilala, mvula ndi mphepo yankuntho, dzombe ndi ngozi zina zachilengedwe zimapereka mpata waukulu kwa mpingo ogawana nawo anthu uthenga wabwino wa Khristu Yesu. Munthawi ya mavuto oterewa anthu amakhala akufunafuna mayankho. Zotsatira zake mitima yawo imakhala yotseguka kwambiri kwa Ambuye. Uthenga wa Chikhristu wa chikondi umapereka chiyembekezo kwa wovulala ndi ozunzika munjira zoterezi. Munthawi zoterezi, inu ndi mpingo wanu mukhale okonzeka kuwafikira ndi chikondi ndi chifundo. Muyang'ane njira zotumikirira iwo amene

[1] Kudzala mpingo kwakambidwa mwatsatanetsatane pa Mutu 39: "Kudzala Mipingo Yatsopano."

ali ndi zosowa. Pamene mukuchita izi, gwiritsani ntchito mpata umenewu kugawana nawo uthenga wabwino.

Kufikira anthu a Chisilamu

Anthu a chipembedzo cha Chisilamu akuchuluka ndi kufalikira mu Afirika monse. Chisilamu chochitila ena zantopola chikutenga malo, chikuononga madela ena mu Afirika. Chifukwa cha ichi, Asilamu ochuluka akukhumudwa ndi chipembedzo chawo. Mpingo wanu upeze njira zofikira asilamu amene sakukhutira nacho chipembedzo chawochi.

Kugwiritsa Ntchito Kulumikizana kwa Ubwenzi

Kulumikizana kwa ubwenzi monga achibale, abwenzi, oyandikana nawo, ndi ogwira nawo ntchito kukhoza kukhala ngati mulatho wachikhalire ofikira otayika ndi uthenga. Izitu ndi zotheka kwambiri makamaka kumadera akumidzi ku Afirika. Kumeneko anthu amakhala moyandikana ndipo amakhala olumikizana ndikugawana zinthu zambiri. Muchikhalidwe choterechi, kutembenuka kwamtsogoleri m'modzi amene amamvera maganizo ake mderalo kumatha kupangitsa kutembenuka mtima kwa anthu ena amene amadziwana naye. Kulalika kudzera mukulumikizana kwa maubwenzi kuli ndi kuthekera kobweretsa anthu ochuluka kwa Ambuye ku Afirika.

Maubale Okhazikitsidwa Apaderadera

Kukhazikitsa ma ubale ofuna kupindula chinachake ndi mipingo komanso mabungwe omwe ali ndi zolinga zofanana ndi zathu ikhoza kukhala njira inanso yamphamvu yofikira otayika ndi uthenga wabwino. Izi zikhoza kukhala zoona makamaka pamene tikugwira ntchito imene tonse tagwirizana mofanana kuti titero. Mpingo wanu ukhoza kupanga ubwenzi ndi mpingo wina kapenanso bungwe lomwe limagwira ntchito limodzi ndi mpingo kuchita dongosolo lapaderadera lofuna kufikira anthu ena ake amene salabadiridwa monga ana amasiye, ana oyendendayenda, kapena amene agweredwa ngozi zogwa mwadzidzidzi.

ZINTHU ZOFUNIKIRA

Pamene pali machitidwe ochuluka pofuna kufikira anthu otayika, kwa Mbusa wa Chipenetekoste, zinthu zitatu izi zofunikira zidzipezeka nthawi zonse: Kulalika

kwa uthenga wabwino, mphamvu ya Mzimu Woyera ndi pemphero lokhudza pamtima.

Kulalika Uthenga Wabwino

Kuti tifikire otayika, uthenga wabwino ukuyenera kulalikidwa (Marko 16:15; 1 Ako. 9:16). Paulo anadziwitsa, "aliyense amene adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka" (Aroma 10:13). Kenako anafunsa mafunso angapo osongoka: "Ndipo iwo adzaitana bwanji pa Iye amene sanamkhulupirire? ndipo adzakhulupirira bwanji Iye amene sanamve za Iye? ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira?" (v. 14). Palibe chipulumutso popanda kumva ndikukhulupirira uthenga wabwino. Monga Mbusa wa Chipentekoste, udzikhala okonzeka nthawi zonse kugawana nawo uthenga wabwino anthu otayika (Aroma 1:15-16). Ndipoukonzekeretse mamembala ako kuchita chimodzimodzi.

Mphamvu ya Mzimu Woyera

Pasapezeka ulendo okalalikira popanda mphamvu ya Mzimu Woyera. Yesu analamulira ophunzira ake, "Mukani phunzitsanianthu a mitundu yonse" (Mateyu 28:19). Koma poyamba anayenera kukhala munzinda kufikira atavekedwa ndi mphamvu yochokera kumwamba (Luka 24:49; fanizila Machitidwe 1:4-8). Machitidwe oterewa a m'baibulo akupitilirabe mpakana lero. Poyamba kupatsidwa mphamvu, kenakano kulalika.

Machitidwe a m'Chipangano Chatsopano olalikira kwa otayika akukhudza kulalikira kodzozedwa kutsatilidwa ndi zizindikiro ndi zozizwa zotsimikizira (Mat. 10:7-8; Marko 16:17). Sikungolalikira uthenga wabwino kokha ayi, komanso mphamvu yake iwonetseredwe. Izi ndi zoona makamaka ku Afirika. Anthu ambiri a ku Afirika, akuchokera m'madera amene muli kupembedza mafano, ufiti, ndi zamatsenga. Amafunafuna chipembedzo chimene chili ndi mphamvu kuposa mphamvu zakumidima

Monga Mbusa wa Chipentekoste wa nzeru, ukuyenera kutsindika za ubatizo wa Mzimu Woyera, utumiki wa mphamvu, ndi chionetsero cha mphatso za Mzimu kumisonkhano yolalikira otayika mawu. Komabe mukuyenera kukhala osamala kuti uthenga wabwino usayikidwe pambali kapena kupeputsidwa chifukwa choti anthuakungofuna zozizwa ndi zizindikiro.

Pemphero loonadi

Pomaliza, chochitika chilichonse pampingo chokhudzana ndi kukalalika kwa otayika chisambitsidwe m'pemphero. Pemphero limenero ndiye chifungulo cha kuchipambano kukulalika kwa otayika. Chochitika chilichonse cha kulalika kwa otayika chimachokera pa ichi (pemphero). Mupemphero, timayitanira pa Ambuye kuti adzaze okhulupirira ndi mphamvu, kutsogoza mapazi awo, kudzoza ulaliki wawo, kuchita zizindikiro ndi zozizwa, ndi kutsekula mitima ya iwo akumva uthenga olalikidwa (fanizilani Machitidwe 4:29-30).

Kufikira otayika ndi uthenga kuli pa mtima pachifukwa chimene mpingo ulipo. Palibe mpingo umene ungadzitchule kuti ndi wa Chipentekoste pamene ukulephera kufikira miyoyo yotayika mu mphamvu ya Mzimu Woyera. Potero, monga Mbusa weniweni wa Chipentekoste udzitsogolera mpingo wako molimba mtima kufikira otayika ndi Khristu.

~ Mutu 38 ~

Kutumikira Dera Lanu

Mbusa wa mpingo waung'ono wa Chipentekoste ku Mmawa kwa Afirika anasunthidwa ndi Mzimu Woyera kuti ayambitse sukulu ya pulayimale m'kalasi ya pa mpingo wake. Anachitira umboni, "Tinkangofuna kuti tithandize ana opezeka m'dera lathu kupeza maphunziro abwino. Timangofuna tichitepo mbali yathu kuthana ndi kusadziwa kulemba ndi kuwerenga komanso umbuli m'dera lathu." Chingakhale analibe ndalama, komanso anali asanayendetsepo sukulu, abusawo anakhulupirira kuti Mulungu anawayankhula. Mwa chikhulupiriro anapita chitsogolo ndiganizolo.

Pozindikira kuti sukuloyo ifuna malo osungilamo katundu ophunzitsira, abusa anachotsa makabati a kunyumba kwawo ndikuwabweretsa kusukuluyi. Kenako anagulitsa katundu wawo wamnyumba ndalamazo ndikugulira polembera, mabuku ndizipangizo zomangira. Kenakano anayambapo ntchito yokhazikitsa masomphenya awo asukulu. Popeza sukuluyi sidakakwanitsa kulipira mlonda, iwo anadzipereka kugwira ntchito yolondera. Munthawi yonseyi, amakhulupirira Mulungu kuti awachilikiza ndi kuwatsogolera. Pang'ono ndi pang'ono, sukulu inachitabwino ndi kukula.

Pamene anthu a m'derali amayang'ana Mbusayu akuthamangathamanga, anasunthika ndi masomphenya ake ndikukhudzika kwawo ndi umoyo wa anthu a m'derali. Chifukwa cha ichi, anayamba kupereka ndalama zothandizira sukuluyi. Popita nthawi, Mulungu anapanga njira kuti mpingowu umange zipinda zina

zowonjezera. Zipinda zatsopanozi anazimanga kolingana ndi mulingo wa boma. Posakhalitsapa, sukuluyi yagula malo ena oonjezera kuti akuze sukuluyi. Abusa analengeza, "Tikukonza zoti timange zipinda zochuluka ndi malo oti ana adzisewererapo. Sitinafikebe pamene Mulungu akufuna kuti tifike, koma Mulungu ndi okhulupilika ndipo akutithandizira kupita chitsogolo. Sukulu yathu ino ndi imodzi mwasukulu zapamwamba m'dera lathu lino tsopano."

Muzonse anachita, abusa ndi ogwira ntchito kusukuluyianakhalabe oona kumaitanidwe a Khristu ogawa uthenga kwa otayika. Chifukwa cha ichi, ophunzira ambiri anakhala a Khristu. Kuphatikiza apo, mafuno abwino amene anabwera chifukwa cha sukuluyi, anatsegula mitima ya makolo ambiri ndipo ambiri analandira Yesu. Mulungu anagwiratsanso ntchito sukuluyi kufikira miyoyo ya Asilamu oyandikira sukuluyi ndi umboni wa Khristu

Ichi ndi chitsanzo chimodzi cha njira zina zochuluka za m'mene inu monga abusa a Chipentekoste mungatsogolere mpingo wanu kuti usamalire dera lanu. Mutu uno uwunikira phunziro limeneli. Ukhazikitsa maziko a Baibulo a utumiki ofikira zigawo zonse za moyo wa munthu; mzimu, moyo ndi thupi. Mutu uno uperekanso maganizo pazinthu zomwe mpingo wanu ungatengere nawo mbali pachisamaliro kudera lanu.

ZOMWE BAIBUBULO LA LAMULIRA

Muzokambirana za utumwi, funso limene limafunsidwa nthawi zina ndi lakuti: Kodi chofunikira kwambiri ndichiti pakati pa kulalika uthenga kwa otayika ndi kusamalira osowa? Yankho ndilakuti, ngakhale kuti palibe chofunikira koposa kutsogolera wina kwa Yesu, mpingo udzichita zonse, usodzi kudera komanso kusamalira osowa kuderako. Zonsezi zikuonetsera kudza kwa Ufumu wa Mulungu. Pamene mpingo wa Chipentekoste wachita bwino pakutsogolera anthu kwa Khristu, ndi kudzala mipingo yatsopano, sunachite bwino kwenikweni pakusamalira opwetekeka

Monga Mbusa weniweni wa Chipentekoste, upewe kuchita zinthu ziwiri zolakwika. Choyamba, pewa kulalikira uthenga usakulabadira mavuto akuthupi a wanthu amene akuzungulira. Komanso, upewe kusamalira anthu kuzosowa zawo zakuthupi popanda kugawana nawo uthenga wabwino. Winawake adalemba bwino kuti "sitinakwanitse kulalikira uthenga wamphumphu wabwino mpakana titaonetsera chikondi cha Khristu." Tiyeni tione bwino lomwe chimene Baibulo limanena za nkhani yofunikirayi.

Kutsata Chitsanzo cha Yesu

Yesu ndiye chitsanzo chathu pa utumiki. Iye amatumikira munthu yense wathunthu, mzimu, moyo komanso thupi. Pamene Yesu amayamba utumiki wake, analengeza cholinga chake. Mzimu wa Ambuye uli [ali] pa Ine" ananena, "chifukwa chake Iyeanandidzoza Ine kuti ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino:anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyenso, kutuLutsa ndi ufulu ophwanyika, kulalikira chakachosankhika cha Ambuye (Luka 4:18-19). Potero, utumiki wa Yesu umadziwika ndi kulalikira uthenga wabwino komanso kusamalira zosowa za anthu.

Mpingo wa m'buku la Machitidwe unatsatira machitidwe amene Yesu anakhazikitsa. Analalika uthenga, kuchiritsa odwala, kutululutsa ziwanda, ndi kusamalira osowa. Chitsanzo chimodzi chosamalira osowa ndi kukhudzika kumene anaonetsa pa amayi amasiye a Chihelene ku Yerusalemu (Machitidwe 6:1). Chitsanzo china ndi kuyankhapo kwa mpingo waku Antiokeya kwa oyera mtima a njala aku Yerusalemu. Atamva mawu a uneneri wa Agabu, "ndipo ophunzira, yense monga anakhoza, anatsimikiza mtima kutumiza zothandiza abale akukhala mu Yudeya; ichinso anachita, natumiza kwa akulu mwadzanja la Barnabasi ndi Saulo (Mach. 11:29-30).

Zochita Ziwiri Zikuluzikulu

Yesu anasiyila mpingo wake ntchito ziwiri zikuluzikulu. Imodzi imatchedwa Kutuma Kwakukulu (Mat. 28:2818-20); yachiwiri ikutchedwa lamulo lalikulu/loposa onse (Mat. 22:34-40). Monga Mbusa okhulupirika wa Chipentekoste utsogolere mpingo wako kumvera zonsenzi. Mu lamulo lalikulu, anatilamulira ife kuti,"mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse." Mu lamulo lalikulu, anatilamulira ife kukonda Mulungu mwapamwamba ndi kukonda anzathu monga ife eni. Mufanizo la Msamariya Wachifundo, Yesu anaphunzitsa kuti mnansi akhoza kukhala wina aliyense amenetakumana naye ndipo akufunika thandizo lathu posatengera mtundu wake kapena chipembedzo. Msamaria wa chifundo anatsimikizira kuti anali mnansi wabwino poyima ndi kuthandiza munthu wovulazidwa. Yesu akutilamulira ife, "pita nuchite iwe momwemo" (Luka 10:37).

Kuunikira kwina kwa Baibulo

M'malo ena angapo, Baibulo limatiuza ife kuti tisamalire iwo amena ali osowa. Mwachitsanzo, Yakobo analemba, "Mapembedzedwe oyera ndi osadetsa pamaso pa Mulungu ndi Atate ndiwo: kucheza ndi ana amasiye ndi akazi amasiye m'chisautso chao, ndi kudzisungira mwini wosachitidwa mawanga ndi dziko lapansi" (Yakobo 1:27). Yesu anaphunzitsa kuti pakutumikira kwa iwo ali ndi zosowa (ndiye kuti., anjala, aludzu, amaliseche, odwala, osowa pokhala, ndi andende), tikutumikira Khristu (Mat. 25:31-40). Pakulephera kuwasamalira iwo, tikunyalanyaza Khristu (vv. 41-46). Pamene mukutumikira kuzosowa za anthu zakuthupi, musamaiwale kuti wina aliyense ali ndi moyo umene udzakhala mpakana kalekale kumwamba kapena kugehena. Usamalephere kugawana nawo uthenga wabwino ndi kuwapatsa mpata oti alandire Yesu.

KUFUNIKIRA KWA KUTUMIKIRA ZOSOWA ZA ANTHU A M'DERA LATHU

Pali phindu lochuluka kwa mpingo wa Chipentekoste m'kutumikira zosowa zam'dera lanu. Tiyeni tiwone ziwiri:

Zimamkondweretsa Mulungu

Mulungu amakondwera pamene ana ake atumikira zosowa za m'dera lawo ndikuwafikira ndi chifundo kwa iwo akukhala malo ozungulira. Tikatero ndiye kuti tikuonetsera chikhalidwe chokonda cha Mulungu ndipo tikutsatira chitsanzo cha Yesu amene anachiritsa onse amene anabwera kwa iye (Mat. 8:16). Mu uthenga wake wa paphiri, Yesu anati, "Munamva kuti kunanenedwa, Uzikondana ndi mnansi wako, ndi kumuda mdani wako: koma Ine ndinena kwa inu, Kondanani nao adani anu, ndi kupempherera iwo akuzunza inu;kotero kuti mukakhale ana a Atate wanu wa Kumwamba; chifukwa Iye amakwezera dzuwa lache pa oipa ndi pa abwino, namavumbitsira mvula pa olungama ndi pa osalungama" (Mat. 5:43-45). Yesu akuti tikonde ndi kufunafuna kudalitsa aliyense— kuphatikizapo adani athu. Tikachita izi, tidzakhala ngati atate athu wakumwamba, ndipo zochita zathu zidzakondweretsa Mulungu.

Zimatsekula Makomo

Kutumikira zosowa za anthu a m'dera lathu sikumango kondweretsa Mulungu kokha, kumaumba mafuno abwino pakati pa mpingo ndi anthu am'deralo. Pamene

anthu a Mulungu awonetsa chikondi kwa ena, anthu amaona, ndipo amayamba kuona mpingowo ndi diso labwino. Yesu adachiritsapo munthu osayankhula. Pamene anthu adamva za mchitidwe wachifundo oterowu, anadabwa kwakukulu nanena, "Wachita Iye zonse bwino; angakhale ogontha awamvetsa, ndi osalankhula awalankhulitsa" (Marko 7:37). Pamene anthu anaona kuti Yesu amawasamalira, mitima yawo inatembenukira kwa Iye. Pamene mpingo wanu udzayamba kutumikira ndi kudalitsa anthu m'dera lanu, anthu adzanena, "anthu abwino aja" pamene anthu akunja adzayamba kuona mpingo wanu mokoma, makomo adzatseguka kukulalika uthenga wabwino.

KUZINDIKIRA ZOSOWA

Kutumikira zosowa za anthu a m'dera lanu kumayamba ndi kuzindikira zosowazo kenako ndikuyambapo kuthandiza. Nazi njira zingapo zimene mpingo wanu ungachite potumikira anthu m'dera lanu:

Sukulu za Chikhristu

Sukulu za Chikhristu ndi njira yotsimikizika imene mpingo ukhoza kutumikira anthu okhala mozungulira mpingowu ndikupititsa patsogolo uthenga wabwino. Mipingo yambiri ya Chipentekoste, ponseponse mu Afirika ikudalitsa anthu ozungulira pokhazikitsa sukulu. Ena anakhazikitsa sukulu za pulayimale m'malo osalidwa. Ena anayambitsa sukulu kuti zipereke kusintha kumadera kumene kwachuluka sukulu zachikunja kapena za Chisilamu. Sukulu zimachita bwino makamaka m'madela amene anthu ake ndi ouma mtima ku uthenga wabwino. Mpingo umene sungakwanitsekukhazikitsa sukulu ukhoza kuyamba ndi kupeza anthu ongodzipereka pakati pa mamembala kuti aphunzitse ana mwa ulele ndikuthandizira pamaphunziro awo.

Ntchito Zikuluzikulu M'dera

Mipingo ina ya Chipentekoste ikudalitsa madera awo kudzera muntchito zabwino zimene akuchita m'maderawo. Akumaona chosowa m'dera, kenakano n'kupanga dongosolo kuti athane ndivutolo. Mwachitsanzo, mpingo ukhoza kudzipereka kupentanso khoma lachipatala chaching'ono. Kapena kukonzetsa mazenera ndi magalasi osweka pa sukulu yam'deralo. Kapena kukonzetsa denga lodontha pa nyumba ya mzimayi wa masiye. Pa mpingo wina wake, azibambo anakhazikitsa gulu lomwe analitchula kuti Asamaliya a Loweruka. Loweruka lilonse mamembala a mpingowu amapita kukathandiza amayi amasiye ndi anthu

ena osowa ndi ntchitozosiyanasiyana. Pali njira zochuluka zimene mpingo ungatumikilire anthu a m'dera lake ndi ntchito zoterezi.

Zaumoyo

Madera ambiri mbali zonse mu Afirika amasowa chisamaliro chokwanira cha zaumoyo. Kutengapo mbali pa chosowa chimenechi, mpingo ukhoza kukhazikitsa chipatala m'deralo. Kugwiritsa ntchito kudziwika kwake, mpingowu ukhoza kuitanitsa ogwira ntchito zaumoyo pachipatalapo. Kapenanso, poyambirira mpingo ukhozakulimbikitsa mamembala ake kuti adzisamalira anthu. Akhoza kuyang'anayang'ana m'dera lozungulira anthu amene ali ndi zosowa zakuthupi. Angathe kumawathandiza kudzera mukuwapempherera machiritso, kuwatonthoza komanso thandizo la zachuma.

Madzi a Ukhondo

Kutengera pa chiwerengero champingo wanu ndi kuthekera kwake pa chuma, mpingo wanu ungafune kupereka madzi a ukhondo kudera lanu posonkha ndalama zokumbira chitsime kapena kukonzetsa chitsime choonongeka.

Kudyetsa ndi Kusamalira Ana

Kunyentchera kwa ana ndi vuto lalikulu m'madera ochuluka mu Afirika. Kumakhudza kakulidwe kathupi ndi ubongo wa miyanda miyanda ya ana ndi achinyamata, ndipo zotsatira zake zimakhudza munthu moyo wake onse. Mipingo ina ya Chipentekoste inakhazikitsa dongosolo lomapereka chakudya kwa ana kamodzi patsiku. Ena anayamba ntchito yomasamalira ana popereka ndalama zochepa. Ndondomeko zimenezi zimapereka mpata kwa makolo kuti akhoza kupita kuntchito uku akudziwa kuti ana awo akusamalilidwa bwino. Dongosolo lodyetsa ndi kusamalira anawa limapereka mwawi kumpingo ogawa uthenga wabwino kwa makolo ndi ana omwe. Izi zimapereka mpata ku mpingo ophunzitsa ana chikhalidwe cha umulungu.

Kupereka Thandizo Lolipilira Ana Sukulu

Ana ndi achinyamata ochuluka mu Afirika ndi anzeru komanso achidwi ndisukulu, komabe makolo awo sakwanitsa kulipira malipiro a sukulu. Mpingo wanu ukhoza kuthana ndi vuto limeneli pokhazikitsa dongosolo lomalipilira ana

anzeru malipiro a sukulu. Izi zidzawathandizira iwo kuti akwaniritse maloto awo ndikupeza luso loyenelera kutukula miyoyo yawo komanso kutukula dela lawo.

Kukuza Achinyamata

Achinyamata amu Afirika amayimilira tsogolo la dziko la Afirika. Nzomvetsa chisoni kuti ambiri a iwo akuthera kudzionong'a ndi mankhwala ozunguza ubongo ndi zikhalidwe zina zoipa. Mpingo wanu ukhoza kuthandizirapo pa chosowa chimenechi pokhazikitsa ndondomeko zopereka zochita zaphindu kwa achinyamata. Zochitikachitikazi zikhoza kukhala monga zamakwaya, matimu amasewera, ndi zina zothandizira mbali zonse zamunthu. Ogwira ntchito/otumikira akhoza kugwiritsa ntchito zochitikachitika za achinyamatazi kuphunzitsa mfundo zofunikira kuti akule ngati mzibambo kapena mzimayi waMulungu. Ndondomeko zimenezi zikhozanso kupereka mpata ogawa uthenga wabwino kwa achinyamata ndikuwatsogolera kwa Khristu.

Maphunziro a Akuluakulu

Anthu akuluakulu ochuluka sanapeze mwayi ophunzira sukulu ya pulayimale kapena sekondale. Mpingo wanu ukhoza kukwaniritsa chosowa chimenechi pokhazikitsa maphunziro kwa anthu achikulire. Maphunzirowa akhoza kuphatikiza zinthu izi:

Maphunziro akuwerenga ndi kulemba. Mpingo ukhoza kuyamba makalasi osalekeza ophunzitsa anthu akuluakulu kuwerenga ndi kulemba. Kuphunzira luso limeneli kudzaonjezera m'mene amadzionera kulemelera kwao ndi kuwathandizira kuti apeze ntchito zabwino. Izi zidzathandizira kupititsa patsogolo moyo wa anthu m'dera lonselo. Ziwakonzekeretsa kuwerenga Baibulo ndi mabuku ena a uzimu amene mpingo ungamagawe kwa iwo. Mpingonso ukhoza kukhazikitsa kalasi yophunzitsa chiyankhulo chachiwiri monga chizungu, chifalansa kapena chipwitikizi.

Kupititsa patsogolo Mabanja. Mabanja ochuluka mu Afirika sakhalitsana bwino, ndipo kuthetsa maukwati kukuchuluka. Anthu a pabanja akuyenera kudziwa mfundo za m'Baibulo zokhudza ukwati. Izitu ndizoona kunja ndimkati mwatchalitchi momwe. Pofuna kuthana ndi vuto limeneli, pofunika kukonza kalasi kapena maphunziro a zam'banja ndi kuitana aliyense ngakhale sapemphera nanu. Mamembala anu akhoza kuyitana abwenzi ndi anzawo osapulumutsidwa kudzakhala nawo pa maphunziro amenewa. Izi zingathandizire iwo kuti azindikire

cholinga cha Mulungu pa banja lawo. Panthawi yamaphunziroyi, uthenga wabwino ulalikidwe, mabanja apatsidwe mwayi olandira Yesu monga mpulumutsi wawo.

Maphunziro akayendetsedwe kabizinezi. Ngati nkotheka, mpingo wanu ukhoza kuyamba kuphunzitsa anthu akulu msinkhu m'mene angayambire ndi kukuza bizinezi komanso kukhala adindo, kuphatikizapo kufunikira kokhala ndi khama pantchito.

Njira zabwino zamalimidwe. Kumadera akumidzi, mpingo ungathe kufuna makalasi kapena misonkhano pa njira zabwino zochitira ulimi. Akatswiri pa ulimu akhoza kuitanidwa kutiadzaphunzitse pamaphunzirowa.

Njira Zina

Izi ndi njira zochepa chabe zammene mpingo wanu ungatumikilire anthu a m'dera lake. Mzimu Woyera angathekukutsogolerani kunjira zina ndi ntchito zina zomwe sizinatchulidwe pano zam'mene mungatumikilire anthu.

KUMEMEZA MPINGO

Mukhoza kumafunsa kuti "Kodi ndingatani monga ine Mbusa wa Chipentekoste kuti ndikhazikitse ntchito zotumikira anthu a m'dera lathu?" Monga mtsogoleri osankhidwa ndi Mulungu, mukuyenera kukhala patsogolo. Mukuyenera kuyambitsa masomphenyawo, kukonza ndondomeko ndi kuyang'anira kagwiridwe ka ntchito yonse monga mwa dongosolo lomwe mwakhazikitsa. Kuti mukhazikitse dongosolo labwino la zochita, lingalirani zinthu izi:

Onani Chosowa

Yesu anaona chosowa poyamba. Anawona kuzunzika kwa anthu amene anamuzungulira ndipo "anagwidwa mtima ndi chisoni chifukwa cha iwo popeza anali okambululuka ndi omwazikana, akunga nkhosa zopanda mbusa" (Mat. 9:36). Kenakano anakhazikitsa dongosolo. Anapempha ophunzira ake, "chifukwa chake pempherani Mwini zotuta kuti akokose antchito kukututa kwake" (v. 38). Panthawi imeneyi, Yesu anawauza iwo, "Kwezani maso anu, muyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta"(Yohane 4:35).

Kumbukirani, musanayambe kukhazikitsa dongosolo loti mulichite, monga Yesu, muyambe kaye mwaona chosowa. Pamene mwaona chosowa, mpamene mungathe kuthandiza mpingo wanu kuti uchite chimodzimodzi.

Dziwani Chifuniro Cha Mulungu

Pamene mwaona zosowa zochuluka mudera lanu, mukuyenera kumufunsa Mulungu, "Kodi ndi zosowa ziti mwa izi mukufuna mpingo wathu uzikwaniritse?" Ngati mudzatsekula mtima wanu kwa Mzimu Woyera, adzakutsogolerani. Adzaika mtolo umene udzakulira kulira pamtima panu ndi kukuonetsani kuti ndizosowa ziti mukuyenera kuzifikira.

Pangani Zinthu Zosavuta

Pamene muyamba kupanga dongosolo la ndondomeko yatsopano, chitani zinthu zophweka poyambirira. Mukuyenera kuyamba ndi ntchito yosavuta kuyikwaniritsa. Pamene mamembala a mpingo wanu awona chipambano pa ntchito yaying'onoyi, adzatakasika kuchita ntchito yovutirapo.

Yambanipo Ntchito

Pamene Mzimu wakusonyezani kuti nthawi yakwana, nthawi yomweyo yambanipo kukhazikitsa ndondomekoyo kudalira Mulungu kuti akutsogolerani pa ndime ina iliyonse.

Chitani za Uzimu

Pamene mukutsogolera mpingo kusamalira zosowa za anthu zakuthupi, muonetsetse kuti simukunyalanyaza zosowa zaku uzimu. Khristu akhalebe chikatikati cha dongosolo lililonse ndi zochita zonse. Inu pamodzi ndi amene mukugwira nawo ntchito mudzipemphera pafupipafupi, kuonetsetsa kuti mukhalebe odzala ndi Mzimu Woyera.

Limbikitsani Mpingo Onse Kutengapo Mbali

Musayerekeze kuchita ntchito yonse nokha. Koma, mumemeze mamembala a mpingo wanu kuti atengepo mbali. Aliyense akhoza kutengapo mbali mwanjira inayake. Monga Mbusa wa Chipentekoste, mupeze mphatso zimene Mulungu anawapatsa mamembala ndi kuwalimbikitsa kuzigwiritsa ntchito kudalitsa ntchito ya Mulungu.

Dalirani Mulungu Kupereka Zofunikira

Pomaliza, mudalire Mulungu kuti akwaniritsa zofunikira zanu. Musadikilire mpakana zonse zofunikira zitapezeka kuti muyambe ntchito. Mukatero, simungayambe. Monga anachitira Mbusa uja tamuona kumayambiliro a mutu uno, muchite zimenemungakwanitse kolingana ndi zimene mulinazo, ndikudalira Mulungu kuti akwaniritsa zinazo. Ngati mukhale omvera kwa Mulungu, ndikukhalabe okhulupilika ku masomphenya amene Mulungu wakupatsani, adzakwaniritsa zosowa zanu zonse (Afilipi. 4:19).

~ Mutu 39 ~

Kudzala Mipingo Yatsopano

Charles anali ophunzira utumiki ku Sukulu ya Baibulo ku M'mawa kwa Afirika. Tsiku lina anati kwa mphunzitsi wake, "ndisanamwalire, ndikufuna ndidzadzale mipingo yokwana zana (100) pakati pa anthu a mtundu wanga." Mtolo wokadzala mipingowu unabadwa mumtima mwake pamene amayenda ndi magulu a utumwi ochokera ku Baibulo sukulu. Gululi linali litadzala mipingo ingapo kumadera a kumidzi pakati pa magulu a anthu amene anali asanafikilidwe. Munthawi imene amayenda kukadzala mipingoyi, Charles anaphunzira njira zatsopano zakadzalidwe ka mipingo yatsopano.

Pamene mpingo wa Assemblies of God unabwera koyamba kudziko lake, anayamba kugwira ntchito pakati pa anthu a mtundu wake. Komabe, patapita zaka zochuluka kunali matchalitchi ochepa chabe pakati pawo. Iye anatsiliza maphunziro ake a Baibulo zaka khumi kudza mphambu zisanu ndi chimodzi (16) zapitazo. Lero, Charles anakwanitsa kukadzala mipingo yopitilira makumi atatu (30). Kudzera muchikoka chake monga mtsogoleri wa mpingo, wapangitsa kuti mipingo ina yoposera makumi asanu (50) idzalidwe. Yonse pamodzi ikupitilira makumi asanu ndi atatu (80). Tsopano Charles waunikiranso mulingo wamatchalichi amene akufuna kudzala. Iye akulumbira kuti, "ndikufuna ndidzale matchalitchi mazana awiri (200) atsopano muzaka khumi (10) zikubwerazi"

Monga momwe amayi athanzi amabereka ana, chimodzimodzinso mipingo yathanzi imadzala mipingo ina. Mpingo uliwonse ukhale odzala mipingo. Mutu

uno uwunikila m'meneBaibulo limayikila poyambirira kudzala mipingo, zitsanzo zakadzalidwe ka matchalichi, mpingo monga gulu la atumwi, mipingo ya utumwi yodzazidwa ndi Mzimu Woyera, mfundozamipingo yodzalidwa ndi anthu akomweko, ndi njira zimene Mbusa wa Chipentekoste angatsatire kuti adzale mipingo.

KUFUNIKIRA KWA MALEMBA

Yesu anati, "ndidzamanga mpingo wanga" (Mat. 16:18). Analamuliranso, "Mukani phunzitsani anthu a mitundu yonse" (28:19). Wina adanena, "Yesu sanatilamulire ife kuti tidzale mipingo, anatilamulira ife kuti tipange akuphunzira." Komabe, onetsetsani mmene ziganizo zili m'mwambazi zikulumikizilana. Kodi wina angapange bwanji ophunzira popanda kudzala mpingo, ndipo wina angadzale bwanji mpingo weniweni popanda kapanga ophunzira? Kufikira otayika popanda kuwakhazikitsa iwo m'mau kuli ngati kubereka mwana ndikumusiya patchire. Kudzala mpingo ndikofunikira kuti ntchito ikhazikike komanso kuti okhulupirira akule.

Atumwi, atumiki ndi ogwira ntchito mu Chipangano Chatsopano anali otsimikizika pakukhazikitsa mipingo. Petro, Yohane, Filipo, amuna aku Kupro, ndi Kurene, Barnabasisi, Paulo, Yohane otchedwa Marko, Sila, Luka, Timoteo, Prisika, Akwila, Gayo, Aristariko, Erasto, ndi Tito, pambali pa ena, onse anachita nawo zodzala mipingo. Amuna ndi akazi amenewa amatsatira lamulo la Khristu loti akapange ophunzira ndipo pochita izi, anadzala mipingo. Monga abusa a Chipentekoste, tikuyenera kuchita chimodzimodzi.

ZITSANZO ZAKADZALIDWE KA MPINGO

Mbusa wachisodzera nthawi ina anayankhulapo kwa mtsogoleri wake wa boma (distrikiti) lake zokadzala mpingo mu tawuni ina yake. Msogoleriyu anayankha, "Mulungu sanandiuze kuti ndikadzale mpingo kumeneko koma ngati ukufuna kudzala, pita. Ngati ikakhazikike, tidzadziwa kuti chinali chifuniro cha Mulungu. Zikakanika, tidzaziwa kuti sichinali chifuniro chake." Pakumva kuti Mzimu akumutsogolera, Mbusa wachinyamatayu anapita kumalo kuja ndikukadzala mpingo wake oyamba. Kuchokera pa nthawi imeneyo, wadzala mipingo yoposa makumi awiri (20).

Mu Afirika yense, amuna ndi akazi ambiri pakumva mayitanidwe kuti akadzale mpingo, anachita chimodzimodzi. Akwanitsa kudzala mipingo paokha,

popanda thandizo kuchokera kwa wina aliyense wakunja. Mchitidwe uwu utha kutchedwa "ukadziotche." Zili ngati bambo kuphunzitsa mwana wake kusambira pomuponyera pathawale lakuya popanda kumuphunzitsa kapena kumulangiza kaye. Pamene mipingo yambiri inayambidwa mnjira imeneyi, sinjira yabwino. Odzala mpingo anachitira umboni ku chimenechi. "Ndinaphunziradi zambiri kuchokera ku mpingo oyamba omwe ndinadzala," anatsimikizira. "Chinthu chimodzi ndinaphunzira ndichakuti sindikufunanso kudzala mpingo wina opanda gulu la anthu ogwira nawo ntchito odzipereka."

Kudzala mpingo ndi gulu lothandizira ndi mtundu wa kadzalidwe ka mpingo umene uli ndi ubwino ochuluka. Tangolingalirani kuti, m'malo motumiza anthu awiri kuti akadzale mpingo, nkutumiza gulu la anthu khumi kapena kuposera apo. Gululi likhoza kuphatikizapo Mbusa watsopano ndi mkazi wake, wotsogolera malambiro, banja lokhwima kuti lizikathandizira kuchita zinthu mwachikulu, ndi anthu othandizira ana ndi achinyamata. Gululi limapereka thandizo lazachuma komanso kuwalimbikitsa pazochitika odzala mpingowo. Kachitidwe kodzala mpingo ndi gulu lothandizira kamathandizira kuti mpingo ufike pokhwima mwansanga. Posakhalitsa, mpingowo umafika poti ukhoza kukadzalanso mipingo inzake.

Kachitidwe kogwiritsa ntchito gulu kukadzala mpingo kamatha kutenga maonekedwe osiyanasiyana. Manthu wa mpingo amatha kubereka mwana (mpingo wina) potumiza Mbusa amene amathandizira Mbusa wamkulu ndi anthu ena kudera loyandikana nalo. Mpingo waukuluwu ukhozano kumapereka uphungu ndi chisamaliro kufikira mpingo watsopanowu utakhazikika. Paulo ndi gulu lake la utumwi ndi zitsanzo zabwino za mtundu umenewu okhala ndi gulu lothandizira limene limayenda ku malo kumene kunali kusanafikiridwe ndi uthenga ndi kudzala mipingo mmalo oti Khristu sakumudziwa.

Ena anakhazikitsa dongosolo lothandizira odzala mipingo kwa chaka kapena zaka ziwiri pamene akupanga zodzala mpingo watsopano. Akatelo, thandizo lija amalichepetsa kenako ndikuliyimitsa pamene okhulupirira atsopanowa akula kukhala ophunzira odzipereka otha kupereka chakhumi chokwanira kuyendetsera ntchitoyo. Mitundu ya kadzalidwe ka mipingo ikuphatikizapo iyi:

- *Kulera:* Mpingo waukulu umakadzala mpingo waung'ono monga tafotokozera pamwambapa.
- *Kuyambitsa:* Oyambitsa kudzala mpingo amatumizidwa kudera latsopano kuti akadzale mpingo.

- *Kudzilekanitsa:* Gulu laanthu lomwe limachokera kutali kapena kudera kumene kuli anthu amitundu yosiyana siyana kuzasonkhana nawo ku mpingo waukulu limapempha chilolezo choti adzilekanitse ku mpingo waukulu ujandikukhala mpingo watsopano.
- *Milaga:* Milaga yomwe imakumana kumbali ina ya mzinda imasanduka kukhala mipingo.
- *Mipingo yogwirizana nayo:* Mipingo ya pasekishoni, padistrikiti, kapena yam'dziko lonse imagwirizana zodzala mipingo.
- *Sukulu Ya Baibulo.* Sukulu yosula azibusa amasonkhanitsa ophunzira kukadzala mipingo yatsopano.
- *Njira Zina:* Njira zina zaluso zingapangidwe kuti mpingo udzalidwe.

Njira iliyonse imene wina angagwiritse ntchito, kudzala mpingo siyophweka. Zimasowekera kudzipereka kuchokera kwa Mbusa watsopanoyo, banja lake ndi gulu lomwe akutsekula nalo mpingowo. M'dani sakondwera kuti mipingo yatsopano idzalidwe chifukwa imalowelera m'mdera lake (Mateyu. 12:29). Adzalimbana kutsutsana ndi mpingo odzalidwawo (Aefeso 6:12). Komabe, odzala mpingo wa Chipentekoste, ali ndi Wamkulu okhala mkati mwake kumthandizira kuti apambane (1 Yohane 4:4).

Monga Mbusa wina aliyense wa Chipentekoste, upemphere ndikukonza dongosolo la mmene ungatsogolere mpingo wako kukadzala mipingo yatsopano, koyandikana nanu kapena kumadera ena osafikilidwa mdziko lanu, angakhalenso kunja kwa dziko lanu mu Afirika kapenanso kudziko lonse lapansi.

MUDZI WA UTUMWI

Mpingo wa thanzi ndi mpingo opereka. Mpingo wa thanzi ndi mpingo ophunzitsidwa bwino za Mulungu. Mpingo wa thanzi ndi mpingo wachidwi pa utumwi. Mpingo wathanzi ndi mpingo ochitira umboni. Mpingo wathanzi ndi mpingo umene umabereka mipingo ina yathanzi. Koma mpingo umabereka bwanji mpingo unzake? Ndipo inu ngati Mbusa wa Chipentekoste, mungatani kuti mukadzale mpingo wina?

Mpingo waku Antiokeya ndi chitsanzo chozindikirika bwino cha mpingo wathanzi, wachindunji pa utumwi. Mpingowu unadzalidwa ndi Ayuda omwe sanali atumiki odzozedwa ochokera kuYerusalemu, Kupro ndi Kurene amene anagawana ndi ena chikhulupiriro chawo molimba mtima, kuphatikizapo anthu a mitundu ina (Machitidwe 11:19-20). Anali mpingo wodzazidwa ndi mphamvu ya

Mzimu (v. 21). Anali ndi utsogoleri wabwino(vv. 22-26). Anali mpingo opereka (vv. 27-30), ndipo anapemphera , anasala ndi kulambira Mulungu (13:2).

Ndipamene Mzimu Woyera anati kwa iwo, "Mundipatulire Ine Barnabasi ndi Saulo ku (utumwi) ntchito imene ndinawaitanirako," anachitadi moteremo (Machitidwe 13:1-2). Anapereka mwa ufulu anthu awo a pamtima kuti achoke akachite ntchito imene Mulungu anawayitanira iwo kuti akachite. Anatumiza Barnabasi ndi Paulo monga atumwi okadzala mipingo (ndime 3-4).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, Mulungu akufuna kuti akugwiritse ntchito "kukonzekeretsa anthu ake ku ntchito ya utumiki" (Aefeso 4:12). Akufuna akugwiritseni ntchito kukadzala mipingo pafupi ndi kudziko lanu lonse komanso kudziko lose lapansi. Mulungu wakupatsa iwe kuthekera ndi danga kulenga mumpingo wako chikhalidwe cha utumwi ndi kudzala mipingo. Ukhoza kupanga izi pakuphunzitsa ndi kuonetsera kapempheredwe ka utumwi, kulambira, utsogeleri, kupereka, kulalika kwa otayika ndi kugwira ntchito limodzi pagulu. Muzochitika-chitika zoterezi, Mulungu adziyitana ndikupereka mphamvu kwa anthu ake kuti atuluke ndikukalalikira uthenga ndi kudzala mipingo yatsopano.

Uyenera kuwaitanira anthu anu kuti apereke moolowa manja kuntchito ya Ambuye, ndipo ulole Mulungu achite chimodzimodzi ndi iwe. Mulungu akhoza kukufunsa iwe kuti upereke mamembala ako apamtima kuti akhale okadzala mipingo. Mphatso imodzi yayikulu ungapereke kwa Mulungu ndiyo kudzutsa anthu mu mphatso zawo ndi kuwatumiza ku utumiki. Barnabasi anathandizira kumudzutsa Paulo (Machitidwe 9:26-27; 11:25). Kenakano anamutumiza iye kuti akachite utumiki payekha ndikukuza gululakelake lochita nalo utumiki (15:36-41).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, mudzi wa utumwi umene ukhazikitse mumpingo wako udzagwira ntchito monga maginito. Mudzi wa atumwi ndi gulu lachindunji pokwaniritsa Kutuma Kwakukulu kwawo komanso kudziko lonse lapansi. Pamene anthu awona Mzimu wa Mulungu akuyenda mumpingo wako, adzafuna kukhala gawo la zimene Akuchita.

Mu Machitidwe 6, kusamvana kunabuka pokhudzana ndi kusalidwa kwa amasiye ena pakugawana zakudya. Atumwi anathetsa kusamvanaku posankha amuna asanu ndi awiri odzazidwa ndi Mzimu Woyera kuti awasamalire iwo. Machitidwe awa anakondweretsa anthu mkati ndi kunja komwe kwa mpingo. Zotsatira zake, "Mau a Mulungu anakula; ndipo chiwerengero cha akuphunzira chidachulukatu ku Yerusalemu; ndipo khamu lalikulu la ansembe linamvera

cikhulupirirocho" (v. 7). Pamene upanga mpingo wako kukhala mudzi wokonda wa utumwi, anthu adzakopedwa kwa Khristu ndi ntchito yake. Kukuza mpingo ndi kudzala mpingo kudzayenda mosavuta mzochitika zamtundu umenewu.

MIPINGO YA UTUMWI YODZALA NDI MPHAMVU YA MZIMU

Machitidwe amatiuza nkhani yolimbikitsa yakupatsidwa mphamvu ku mpingo waku Yerusalemu. Pamene Mzimu Woyera anadza ndikudzaza ophunzira zana ndi makumi awiri (120) aja, khamu linaona chinachake chodabwitsa. Ophunzirawa anayamba kuyankhula ndi malilime ena monga mmene Mzimu anawapatsa kuthekera (2:1-4). Kunali kukwaniritsidwa kwa lonjezano la Yesu mu Machitidwe 1:8. Makamuwo omwe anali odabwitsika anasunthira komwe kunali ophunzirawa. Izi zinampatsa Petro mwai oti alalikire uthenga wabwino mu mphamvu ya Mzimu, kupherezera mukulapa kwa amuna zikwi zitatu (3000)

Mulungu nthawi zina amagwiritsa ntchito zizindikiro ndi zozizwa kuti atakase chidwi chakumvera mau a Mulungu. Ndikofunika kuzindikira kuti m'mabuku a uthenga abwino ndi m'buku la Machitidwe zozizwa zochuluka zinachitika kunja kwa nthawi ya chipembedzo kusiyana ndi nthawi yamapemphero. Ku Machitidwe, chozizwa chimakopa anthu ndi kupereka mpata oti alalikidwe uthenga. Izi zinachtika ku Yerusalemu ndi Petro (Machitidwe 2), ku Kupro ndi Paulo ndi Barnabasi (13:4-12), ku Aefeso ndi Paulo ndi Sila (16:11-40), ndi panthawi zina zochuluka (9:32-35;9:36-43;10:1-11:18; 14:8-20; 19:1-21-20:1).

Mulungu akufuna iwo amene ali kunja kwa mpingo kuti awone mphamvu yake yochita zozizwa ndi chikondi, ndi kutembuka kumtsata iye. Musaononge chozizwa. Nthawi ina iliyonse Mulungu akachita chozizwa, chigwiritseni ntchito ngati mwai oti muuze ena za Yesu.

Yesu ananena kwa Akuphunzira ake: "Monga Atate wandituma ine, inenso ndikutumani inu" (Yohane 20:21). Koma Atate anamutuma bwanji Yesu? Anatumiza mwana wake kuti atumikire mu mphamvu ya Mzimu. Pamene Yesu amayamba utumiki wake, analengeza, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, Chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, ndi akhungu kuti apenyanso, kutulutsa ndi ufulu ophwanyika, kulalikira chaka chosankhika cha Ambuye" (Luka 4:18-19). Yesu anatumikira mu mphamvu ya Mzimu (Machitidwe 10:38), ndipo anatumiza akuphunzira ake kuti akachite chimodzimodzi (Luka 24:46-49; Machitidwe 1:8).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, mukuyenera kukhala odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo mwadaladala kuzani mpingo wanu ukhale thupi la utumwi lodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Poonjezera apo, mwadala mudzale mipingo ya utumwi yodzala ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Mpingo wa utumwi odzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ndi mtundu wa mpingo umene Yesu anadzala. Ndi mtundu wa mpingo umene timauwerenga m'buku la Machitidwe.

Yesu anafotokera kufunikira kwa mpingo wamtundu umenewu mu Machitidwe 1:8 kumene anati, "Komatu mudzalandira mphamvu Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, ndi mu Yudea monse ndi mu Samariya, ndi kufikira malekezero ake a dziko." Potero, mpingo wa utumwi umene uli odzazidwa ndi Mzimu Woyera uli ndi zizindikilo ziwiri izi: mamembala ake ndi odzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ndipo ndi odzipereka ku cholinga cha Mulungu. Ndi mpingo umene umadzala mipingo inanso ya utumwi imene ili yodzazidwanso ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, ndipo ndi yodzipereka kufikira iwo amene sanafikiridwe ndi uthenga m'dziko komanso kudziko lonse lapansi. Mpingo wamtunduwu tiukuze, ndipo ndi mpingo umene tikuyenera kudzala.

MFUNDO ZA MIPINGO YA ENI NTHAKA

Kuzungulira dziko lonse lapansi, Mpingo wa Chipentekoste wakula paliwiro lodabwitsa kwambiri. Chimene chathandizira kwambiri kukula kumeneku ndi kudzipereka kwake kwa mpingowu ku chimene chikutchedwa kuti "Mfundo za mpingo wa eni nthaka." Ichi ndi chikhulupiriro chakuti mpingo uliwonse watsopano ukuyenera kukhala odzidalira okha, odziyang'anira okha komanso odzikukulitsa okha pasanapite nthawi yayitali chiudzalireni. Pamene inu ndi mpingo wanu mupita kukadzala mipingo, muonetsetse kuti mipingoyo ikule ndikukhala yodzithandiza yokha, yothakudzisamalira, kufikira otayika, komanso yakutha kudzala mipingo ina ya utumwi yodzazidwa ndi Mzimu Woyera.

Pamene khanda labadwa m'banja, makolo amalisamalira pachosowa chilichonse. Koma pamene mwanayo akukula ndi kukhwima nsinkhu, makolo amayamba kumuphunzitsa mwanayu m'mene angadzisamalilire. Mwanayu amaphunzitsidwa kuti azikhala bwanji ndipo popita nthawi, amapatsidwa udindo ochuluka wodzisamalira yekha. Pamene mwanayu akula ndikukhala wa nsinkhu, makolo amamumasula iye monga odzidalira yekha komanso kuthandizapo pazochitika m'dziko.

Ndi chimodzimodzi pakudzala mpingo watsopano. Pachiyambi, mpingo obereka unzakewo umapereka nthawi yochuluka ndi zofunikira zambiri pakusamilira khanda lampingoli. Ukhoza kuthandiza ndi utsogoleri, zachuma, ndi ogwira ntchito. Mpingo watsopano umayembekezeka kuti ukule ndi kukhwima. Cholinga ndi chakuti, posakhalitsa ukhala odzidalira okha nkukhala umodzi mwa mipingo yothandiza mu Ufumu wa Mulungu.

CHIYANI TSOPANO?

Mukhoza kumafunsa, "Kodi ndingatani kuti ndikhazikitse mfundo zodzalira mpingozi mu utumiki wanga komanso m'moyo wa mpingo wanga? Ndingakuze bwanji mpingo wanga kukhala thupi lodzala mipingo lamphamvu." Lingalirani kuchitapo izi:

Pempherani

Yambani ndi pemphero lamphamvu. Moona mtima mpempheni Mulungu kuti akupatseni masomphenya odzala mipingo. Pemphani Yesu, Ambuye wa Kholola kuti "kwezani maso anu nimuyang'ane m'minda, kuti mwayera kale kufikira kumweta" (Yohane 4:35). Pembedzerani madera ozungulira amene alibe mipingo ya utumwi yodzazidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (Mateyu. 9:38). Koma musalekele pomwepo. Muyang'anenso madera akutali, kwa anthu ndi malo amene sanafikiridwe m'dziko lanu ndi malo amene kuli umboni wa uthenga wabwino ochepa kapena kulibiretu. Ndipo osayiwala kuyang'ana kumayiko. Pamene mukupemphera, mupemphe Mulungu "Ndi ati mwa anthu ndi Malo amene mukufuna ife tiwafikire ndi uthenga wabwino wa Khristu?"

Dziperekeni

Chotsatira, dziperekeni nokha ndi mpingo onse kwa Mulungu ndi kuntchito yake. Pangani chisankho chokhala mpingo odzala mipingo mwamphamvu.

Ikizani mwa Anthu

Pamene mwadzipereka kukudzala mipingo, yambani kuphunzitsa mamembala ampingo wanu kuti akhale ophunzira a Khristu odzipereka kwathunthu. Lalikirani, phunzitsani, ndipo yankhulani pafupipafupi za cholinga cha Mulungu ndi kulamulira kwa Khristu koti tidzale mipingo. Ponyani masomphenya akudzala mipingo kwa atsogoleri komanso mpingo onse. Pamene

mukuchita izi, perekani mwai kwa iwo amene ali ndikuthekera kwa utsogoleri kuti azitumikira ndi kukuza mphatso zimene Mulungu anawapatsa.

Sonkhanitsani Gulu

Panthawi yoyenera, sonkhanitsani gulu la anthu lokadzala nalo mpingo. Sankhani kuti ndi ndani azikatumikira monga Mbusa wa mpingo watsopanowo. Komanso, sankhani anthu amene adzikagwira ntchito ndi abusawo pagulu la anthu okadzala mipingo. Onetsetsani kuti membala aliyense akudziwa udindo wake. Komanso onetsetsani kuti membala aliyense wagululi ndiwodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Kuonjezera apo, ndikofunikira kuti mukhazikitse gulu lothandizira limene likhalebe kumpingo waukulu kuthandizira mpingo watsopano ndi chilimbikitso, mapemphero ndi chuma.

Khazikitsani Dongosolo

Tsopano, limodzi ndi gulu lanu, yambani kukonzeratu dongosolo. Mudongosolo limeneli mukuyenera kuyankha mafunso awa: "Ndiliti ndipo ndikuti kumene tikadzale mpingo watsopano? Ndindani amene adzachite nawo? Ndizinthu ziti zodziwikiratu zimene tidzachite?" Dongosolo lanu liphatikizepo ndalama zimene zingafunikire ndi zinthu zimene zidzafunike ndikuti muzipeza bwanji.

Yambanipo Kuchita kanthu

Pamene mwatha kupemphera ndi kukonza dongosolo lanu, yambanipo mwamphamvu kuchita zimene mwazikonzazo. Chitani mwachikhulupiriro, kukhulupirira kuti Mzimu wa Ambuye akupatsani mphamvu ndi kudzoza umboni wanu. M'dalireni Mulungu kuti akatsimikiza mawu amene mukalalike ndi zozizwa, zizindikiro ndi zodabwitsa. Pamene anthu akupulumutsidwa, onetsetsani kuti adzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kuphunzitsidwa zoyambirira za kutumikira Khristu. Muyenera kuwamemeza kuti afikire mabanja awo ndi abwenzi awo..

Unikirani

Chotsiriza, pamene mwamaliza ntchito yanu yodzala mpingo, sonkhanitsani gulu lanu lija ndi kuunikira ntchito yonse. Funsani, "Ndichiyani chimene tinachita bwino? Ndichiti chimene tikanatha kuchichita bwino? Nthawi zonse padzakhala zinthu zimene sizinachitike bwino, koma osagwetsedwa mphwayi. Gwiritsani

ntchito zinthu zomwe mwaphunzira kulimbikitsa chikonzero cha ulendo otsatira okadzala mpingo.

Kupanga mpingo wanu kukhala chimango chodzala mipingo, sikungothandizira kupititsa patsogolo cholinga cha Khristu padziko lapansi, kubweretsa chitsitsimutso ku mpingo. Mpingo wanu ukhala okondwera kuti ulimbali yopita kukadzala mipingo yatsopano ndi kuona anthu akubwera kwa Yesu. Mbusa aliyense wa Chipentekoste adzipereke yekha mwachimwemwe kukudzala mipingo yatsopano.

~ Mutu 40 ~

Kukhazikitsa Dongosolo La Utumwi La Mpingo Wapamalo

Nthawi idakwana yoti Yesu adziulule kuti ndi ndani ndikuti anadza chifukwa chiyani. Ngati akuphunzira ake khumi ndi awiriwo akanati adzapitirize ntchito yake iye atapita, anayenera kumvetsetsa choonadichi. Atafika pamalo odekha kunja kwa mzinda wa Kaisereya Filipi, Yesu anawakhazika pansi ophunzira ake. Kutembenukira kwaiwo anawafunsa, “Anthu anena kuti Mwana wa munthu ndiye yani?” Mmodzi mmodzi akuphunzira anayankha, “Ena ati, Yohane Mbatizi; koma ena, Eliya; ndipo enanso Yeremiya, kapena mmodzi wa aneneri.”

Yesu anawafunsano mwachindunji, “Koma inu mutani kuti Ine ndine yani?” Mukaphindi kotsogozedwa ndi Mzimu Simoni Petro anayankha mofulumira, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo!”

Kumuyang’ana mwakuya mmaso mwake, Yesu anamuuza Petro, “Ndiwe wodala, Simoni Bar-Yona: pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululira ichi, koma Atate wanga wa Kumwamba.” Kenako Yesu anawonjezera kuti, “Ine ndinena kwa iwe, kuti iwe ndiwe Petro, ndipo pa thanthwe ili ndidzakhazika Mpingo wanga; ndipo makomo a dziko la akufa sadzaulaka uwo” (onani Mateyu 16:13-20).

Yesu adaulula kwa ophunzira ake kuti anali ndani: Anali Mesiya olonjezedwayo, mwana wa Mulungu. Anawauliranso iwo chifukwa chimene Iye adabwerera: kudzamanga mpingo wake. Anapitilira kuuluranso kuti mpingo umene amaumanga udzakhala oposa bungwe la anthu; udzakhala gulu lokhazikitsidwa mwa uMulungu. Udzakumana ndi kutsutsa kolimba kwa ziwanda, ndipo udzapambana.

KULUMIKIZANA NDI CHOLINGA CHA MULUNGU

Cholinga choyambirira cha Ambuye wathu kwa Mpingo Wake ndi chakuti ulalikire uthenga wabwino wa chipulumutso mwa Khristu Iye asanabwerenso kuchokera kumwamba. Yesu anayankhula chonchi: "Ndipo uthenga uwu wabwino wa Ufumu udzalalikidwa pa dziko lonse lapansi, ukhale mboni kwa anthu amitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimaliziro" (Mat. 24:14). Izi pokhalazoona, Mbusa aliyense wa Chipentekoste ali ndi udindo otsogolera mpingo wake kuti utenge nawo mbali kwathunthu pa cholinga cha Mulunguchi. Mutu uno uwunguza m'mene mungakwanitsire cholinga chapaphatachi cha mpingo.

Kudzikonzekeretsa Wekha

Musanayesere kulumikizitsa mpingo wanu ku cholinga cha Mulungu, mukuyenera kudzikonzekeretsa nokha pa ntchitoyi. Mukhoza kuchita izi munjira izi:

1. Kuzindikira Cholinga cha Mulungu. Poyamba, chikhale cholinga chanu kuti mukhale ndi kumvetsetsa kwabwino kwa cholinga cha Mulungu. Kuti muchite izi, mukuyenera kudziwa kuti cholinga cha Mulungu ndi chiyani ndipo chikugwirizana bwanji ndi mpingo. Cholinga cha Mulungu, nthawi zina chimatchedwa kuti *missio Dei,* ndicho mutu olunzanitsa wa Malemba. Ndicholinga cha Mulungu kuombola ndi kudziyitanira anthu kwa Iye yekha kuchokera kumtundu uliwonse, chinenedwe ndi fuko padziko (Chivumbulutso 5:9; 7:9). Ndicholinga cha Mulungu, mwa Khristu, kuti mbeu ya Abrahamu, "anthu onse apadziko lapansi adzadalitsidwa" (Gen. 12:3; 22:18; Agal. 3:16). Baibulo ndi nkhani ya Mulungu yakuchitachita mu mbiri yadziko kukwaniritsa cholinga chake.

2. Kumvetsetsa Udindo wa Mpingo. Mopitirira apo, monga Mbusa weniweni wa Chipentekoste, mukuyenera kumvetsetsa chikatikati cha udindo wa mpingo mukukwaniritsa cholinga cha Mulungu. Yesu analumikiza mpingo kucholinga cha Mulungu pamene analamulira omutsatira, "chifukwa chake phunzitsani anthu a mitundu yonse ndi kuwabatiza m'dzina la Atate, ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu" (Mateyu 28:19-20; onani Marko 16:15; Luka 24:46-48; Yohane 20:21; Machitidwe 1:8). Lamulo ili la Yesu limatchedwa Kutuma Kwakukulu. Utumwi si chikonzero chabe cha mpingo, ndi cholinga cha Mpingo.

3. Kuvomera udindo wa ubusa. Pomaliza, monga Mbusa weniweni wa Chipentekoste, mukuyenera kuvomereza udindo omemeza mpingo kuti utengeko mbali mu cholinga cha Mulungu. Mukhale "wantchito okhulupirika ndi wa nzeru" amene mbuye wake anamulamulira kuti ayang'anire nyumba yake "kuti awapatse chakudya panthawi yake" (Mateyu 24:45). Kumbukira, tsiku lina mudzadziwerengera mlandu kwa Mulungu mmene munasamalira mpingo wa Khristu (Luka 16:2).

Chitsanzo cha m'Baibulo

Baibulo limatipatsa ife chitsanzo chomveka bwino cha m'mene mpingo weniweni wa Chipentekoste ukuyenera kuonekera. Ukuyenera kukhala mpingo wa utumwi. Mpingo wa utumwi ndi mpingo umene uli odzipereka kupititsa patsogolo cholinga cha Mulungu padziko pano. Mpingo wa ku Antiokeya, Siliya, unali umodzi mwa mipingo yotereyi (Mach. 11:19-20; 13:1-4). Luka anatsirizitsa nkhani ya mpingowu mu Machitidwe monga chitsanzo chokhalitsa cha mmene mpingo ungalumikizirane ndi cholinga cha Mulungu. Ndi chitsanzo chammene mpingo wa Chipentekoste uyenera kuyendera lero lino. Kuunikira kwa ndime ziwiri zimenezi kukuonetsera makhalidwe asanu ndi awiri a mpingo wa utumwi:

1. Kupezeka komanso mphamvu ya Mzimu Woyera. Mpingo weniweni wa utumwi umazindikira kufunikira kwake kwa kupezeka komanso mphamvu ya Mzimu Woyera. Baibulo limanena za mpingo wa ku Antiokeya, "Ndipo dzanja la Ambuye linali nawo" (Machitidwe 11:21). Iyi ndi njira ina yonena kuti Mzimu Woyera amagwira ntchito mwamphamvu pakati pawo (fanizilani 2 Mafumu 3:15; Ezekiele 3:14). Potsatira Mzimu kugwira ntchito mwa iwo komanso kudzera mwa wokhulupirira aku Antiokeya, ndi chidwi chawo pakupindula miyoyo yotayika, "unyinji unakhulupirira natembenukira kwa Ambuye."

2. Atsogoleri a uMulungu, odzozedwa ndi Odzala ndi Mzimu. Mpingo wa utumwi weniweni umatsogozedwa ndi atsogoleri aumulungu, odzozedwa komanso kudzazidwa ndi Mzimu monga Barnabasi ndi Saulo (Machitidwe 11:22-26). Baibulo likuti Barnabasi anali "munthu wabwino, ndi wodzala ndi Mzimu Woyera ndi Chikhulupiriro" (v. 24). Saulo, amenenso anatsogolera mpingo ku Antiokeya, anali odzala ndi Mzimu Woyera ndi chikhulupiriro (13:9; fanizilani 9:17-18).

3. Amasomphenya oyang'ana kunja. Mpingo wa utumwi weniweni mwadaladala umafikira anthu okhala mumzinda kapena m'mudzi mwao. Umu ndi m'mene mpingo waku Antiokeya unachitira. Kuonjezera apo, iwo amafikira anthu amitundu yosiyanasiyana, kulunjika kwa Ayuda komanso amitundu (Machtidwe 11:19-21). Mpingo wa ku Antiokeya unadzalanso mipingo ina mchigawocho (15:41). Kuphatikiza apo, anatumiza atumwi ku maiko ena (13:1-4). Anakhala olumikizana ndi iwo amene anawatuma (14:27).

4. Kulalikira molimba mtima. Mpingo weniweni wa utumwi udzalalikira molimba mtima "uthenga wabwino wa Ambuye Yesu" monga unachitira mpingo waku Antiokeya (Machitidwe 11:20). Kulalikira uthenga wabwino molimba mtima chinali chikhalidwe cha ophunzira mubuku lonse la Machitidwe (fanizilani 8:4-5; 16:30-32; 28:31).

5. Dongosolo-lamaphunziro okhazikika a utumwi. Mpingo weniweni wa utumwi udzaphunzitsa mamembala ake mwatsatanetsatane pa cholinga. Baibulo limati "chaka chonse anasonkhana pamodzi mumpingo, naphunzitsa anthu aunyinji" (Machitidwe 11:26). Ndithudi anaphunzitsa zinthu zoyambirira zoyenera kuti munthu akhale m'Khristu. Komanso, pakuyang'ana mmene mpingo waku Antiokeya umachitira, ndizoonekeratu kuti anaphunzitsa zokhudzana cholinga cha Mulungu ndi mmene Akhristu akanatengera nawo mbali mwamphamvu.

6. Machitachita aufulu a mphatso za Mzimu. Mpingo wa utumwi weniweni udzalimbikitsa machitachita a mphatso za Mzimu pakukumana kwao. Mpingo waku Antiokeya unalimbikitsa machitachita oterewa (fanizilani Machitidwe 11:27-28). Akhristu kumeneko anadalira pa Mzimu wa Mulungu kuti awatsogolere m'chifuniro cha Mulungu. Chionetsero cha mphatso ya uneneri mumpingo kunalimbikitsa kukhazikitsa ndi kutumiza kwa Barnabasi ndi Paulo monga atumwi kwa amitundu (13:2).

7. Kuolowa manja kutakasidwa ndi Mzimu. Mpingo weniweni wa utumwi ndi mpingo opereka moolowa manja. Ku Antiokeya, Akhristu anapereka moolowa manja kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu. Anachitapo kanthu ku uneneri wa Agabu popereka zothandizira abale ndi alongo okhala ku Yudea (Machitidwe 11:29). Izi zikutikumbutsa zomwe zinachitika atatsanulidwa Mzimu Woyera pa Tsiku la Pentekoste (2:44-45).

Monga Mbusa wa Chipentekoste, mugwiritse ntchito mpingo waku Antiokeya monga ngati chitsanzo. Mupange zoti muonetsetse kuti makhalidwe asanu ndi awiriwa a mpingo wa utumwi adzalidwa mumpingo umene mukuutsogolera

KUCHITA CHOLINGA CHA MULUNGU

Mukhoza kumafunsa, "Ndingayambitse bwanji dongosolo la utumwi la mphamvu pampingo wanga? Ndi ndime zanji zimene ndingatenge kuti ndisunthe mpingo wanga kuchokera pamene uli lero kuti ufikire pamene Mulungu akufuna kuti ukhale?"

Kuti muchite izi, mukuyenera kumvetsetsa kuti mpingo wa utumwi sungapangidwe munthawi yochepa. Sizilingati kuti ungokhethemula poyatsira magetsi kenakano mosakhalitsa "kuwala kwa utumwi" kwabwera mu mpingo nthawi yomweyo. Kupanga mpingo kuti ukhale wa utumwi, zimatenga nthawi ndi khama. Zimafunikira chikonzero. Ndipo chikonzerocho chidzasoweka kuti uyambekuchichita.

Nazi njira zisanu za mphamvu zimene mungathe kuzigwiritsa ntchito kuti mulonge masomphenya a utumwi mumpingo wanu. Ngati mungagwiritse njira zimenezi, nthawi zonse; osadukiza, popita nthawi, mpingo wanu udzasuntha kuchoka pakukhala ongoyang'ana mkati, ongosamalira za iwo okha kukukhala mpingo oyang'ana kunja, mpingo wa utumwi—mtundu wa mpingo umene umakondweretsa Mulungu.

Kulalikira Kokhudzidwa

Njira yoyamba imene mungagwiritse ntchito ndi kulonga masomphenya a utumwi ndikudzera mukulalikira kokhudzidwa. Mudzilalikira pafupipafupi pa cholinga chimodzi ndi za udindo wa mpingo kuchita utumwi. Ndipo mulole kuti kukopeka mtima kwanu pa utumwi kudziwike pamene mukulalikira uthenga. Anthu adzasunthika ndi kukopeka mtima kwanu pankhaniyi monga mmene

angasunthikire ndi mfundo zanu zosanjidwa bwino. Potseka uthenga wanu, onetsetsa kuti mwawabetchera anthu a Mulungu kuti adzipereke okha ku cholinga cha Mulungu. Kenakano, itanitsa kuyankhapo kwapaderadera.[1]

Pemphero la Chindunji

Njira yachiwiri imene mungagwiritse ntchito kulonga masomphenya a utumwi kumpingo wanu ndi mapemphero olunjika pa utumwi. Kawirikawiri mudzitsogolera mpingo wanu kumapemphero akholola (fanizilani Mateyu 9:37-38). Mupereke nthawi pa la Mulungu lililonse kumapemphero a utumwi. Munthawi imeneyi, inu kapena mtsogoleri amene mungamusankhe adzitsogolera mapemphero kupemphelera mmodzi mwa atumwi kapena ndondomeko ya utumwi imene mpingowu ukuthandizirapo. Mudzipempherenso anthu amene sanafikilidwe komanso malo mudziko lanu ndi kulikonse m'dziko lonse lapansi.

Kuphatikiza apo, mudzitsogolera anthu anu m'mapemphero kuti Mzimu Woyera atsanulidwe pa mpingo. Pamene mamembala ochuluka adzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu wa Utumwi, mitima yawo idzazidwa ndi chikoka pa otayika. Ndipo Mzimu udzawasintha iwo kuti achitepo mbali yawo kufikira anthu otayika kumadera kwao komanso kumalekezero adziko (Machitidwe 1:8).[2]

Ziphunzitso za Mwatsatanetsatane

Chachitatu, mungathe kulonga chidwi ku utumwi kudzera muziphunzitso zokhudza utumwi zosanjidwa bwino. Kuti muchite ichi, muyenera kuyenda m'malemba ndime ndi ndime kuunikira mmene Mulungu anachitira mumbiri kuti akwaniritse cholinga chake padziko. Maonedwe atsopanowa pa Baibulo adzalenga mkati mwa mitima ya anthu kumvetsetsa kwabwino kwa chikhalidwe cha utumwi cha mpingo. Kumvetsetsa uku kudzalimbikitsa iwo kuti atengepo mbali kwathunthu mu cholinga cha Mulungu.[3]

---

[1] Buku lotchedwa, *Kulalikira Khristu ku Maiko: Ndondomeko zama Ulaliki 100 pa Utumwi Opatsidwa Mphamvu,* lilipo kudzera ku bungwe la Africa's Hope, Acts 1:8 Initiative. Likhoza kupezeka mwaulere pa webusaiti ya www.DecadeofPentecost.org

[2] Zambiri pa mitu iyi, onani Mutu 8: "Kufunikira kwa Pemphero" ndi Mutu 11: "Amalimbikitsa Moyo ndi Kachitidwe ka Chipentekoste."

[3] Mukhoza kuphunzira zambiri zokhudza cholinga cha Mulungu mu buku la Chiyembekezo Cha Afirika Mndandanda Wakupeza Chidziwitso, *Chiphunzitso cha M'baibulo cha Utumwi,* lolembedwa ndi Paul York.

Dongosolo la Daladala

Njira ya chinayi imene mungaikizire masomphenya a utumwi mwa anthu anu ndi kukhazikitsa (kukonzanso) chikonzero mwadaladala kuti mpingo wanu utengepo mbali. Kuti uchite izi,uyenera kuganizirapo mwakuya chigawo chilichonse cha mpingo ndi mautumiki kuti uonetsetse ndondomeko zawo zikuthandizira kuwonetsera kudzipereka kwa mpingo wanu ku utumwi. Iwe pamodzi ndi gulu la atsogoleri a mpingo mufunse utumiki uliwonse pampingo kuti, "Kodi dongosolo ili likuthandiza bwanji mpingo wathu kukwaniritsa cholinga cha Mulungu?" Ngati dongosololo silikuthandiza mpingo kukwaniritsa cholinga cha Mulungu, ichotsedwe or ikonzedwenso.

Maubwenzi a Phindu

Njira yachisanu imene mungagwiritse ntchito kuti mulonge masomphenya a utumwi mumpingo wanu ndikupanga ma ubale ndi atumwi ndi magulu a utumwi odziwika bwino. Palibe mpingo wakudera ungakwanitse kuchita utumwi paokha. Utumwi ndichinthu chimene thupi lonse la Khristu lidzichitira limodzi. Potero, limodzi ndi chikonzero cha mpingo wakudera ofikira anthu, tsogolerani mpingo wanu kugwirizana ndi chikonzero cha utumwi cha mpingo mdziko lanu lonse ndi mabungwe ena ovomerezeka ochita za utumwi. Pochita ichi, mutsogolere mpingo wanu kuthandiza mokhulupirika chikonzero cha utumwi cha mpingo wadziko lanu lonse ndi atumwi amene mpingowo umawavomereza. Pamene mamembala anu adzaona zonse zikukwaniritsidwa kudzera mukugwirira ntchito limodzi kotereku, adzalimbikitsidwa kuti atengepo mbali mochuluka.

Kutengera Mpingo ku Malo a Utumwi

Chomalizira, mukhoza kulonga masomphenya a utumwi ku mpingo wanu, pakuwatengera kudera komwe kukukachitikira utumwi. Nazi njira zisanu zamphamvu zomwe mungachitire zimenezi:

1. Kuchereza alendo omwe ndi atumwi. Njira imodzi imene mungaonetsere mpingo kuzochitika za utumwi ndi pakuitana alendo autumwi kuti abwere adzalalikire kumpingo wanu. Atumwi adzagawana ndi mpingo wanu masomphenya awo ofikira otayika, komanso zimene amakumana nazo pantchito yawo. Pamene anthu adzamvera atumwiwa, kukopeka mtima ndi utumwi kudzabadwa mkati mwao. Pamene muyitana mtumwi kuti adzayankhule, onetsetsa kuti mpingo wanu wamudalitsa mtumwiyo moolowa manja,

kudzipereka kumthandiza mwezi ndi mwezi ndi chuma, komanso kuwapempherera kosalekeza.

2. Lamulungu la Utumwi. Njira ina yamphamvu imene mungawonetsere mpingo wanu ku zochitika ku utumwi ndi pakusankha lamulungu limodzi pamwezi mkulitchula "Lamulungu la Utumwi." Patsiku limeneli, inu kapena munthu amene mwasankha, adziwerenga malipoti ochokera kwa atumwi ndi kuwapempherera. Kenako mudzilalika uthenga wa utumwi ndi kutolera chopereka cha utumwi. Njira iyi idzaonetsetsa kuti mpingo wanu ukusunga thumba la utumwi lathanzi.

3. Msonkhano wa Utumwi. Mukhozanso kufuna kukonza msonkhano wa utumwi wa pachaka. Misonkhano ya utumwi ndi mndandanda wa mapemphero okonzedwa ndi cholinga chozindikiritsa mpingo za utumwi ndi kuonjezera mtolo wake pa otayika. Pamsonkhanowu, mumayitana atumwi kudzatumikira ndikugawana nawo mpingo utumiki wawo. Komanso, pamsonkhanowu, mumaonetsera zimene mpingo wanu wakwaniritsa pankhani ya utumwi pamodzi ndi zimene mukufuna muzifikile pa utumwi mchaka chikudza. Kuonjezera apo, mukufunika kubetchera anthu kuti adzipereke kapena apange malonjezano woti adzipereka mwezi ndi mwezi ndalama zothandizira ndondomeko ya utumwi pa mpingopo.

4. Thabwa lokhomapo za utumwi. Mukhozanso kuonetsera za utumwi kumpingo pokonza ndi kupachika thabwa lachikoka lopachikapo zoonetsera utumwi ndi kuliyika malo oonekera bwino. Pathabwa limeneli pakhomedwe zithunzi za atumwi ndi mawu ofotokozera utumiki wawo. Makalata ochokera kwa atumwi, mapu a malo autumwi ndi zinthu zina zofotokozera zochitika mu utumwi zikhozanso kukhomedwapo pa bolodi lazidziwitso limeneli.

5. Ulendo waku utumwi. Njira ina imene mungaonetsere utumwi kumpingo wanu ndi pakulimbikitsa mamembala anu kuti atengepo mbali pa misonkhano yofikira anthu ya utumwi imene mpingo ukuthandizapo. Mwachitsanzo, nthambi ya utumwi pampingopo ikhoza kufuna kukhala ndi chikonzero chokadzala mpingo kumalo a anthu a mtundu winawake amene ndi osalidwa mudziko lanu. Kapena atha kuthandizapo popereka ndalama kuchikonzero chokadzala mpingo kudera lina losafikiridwa ndi uthenga. Kuonetsera mpingo mwachindunji chonchi kudzathandizira kupititsa patsogolo ufumu wa Mulungu, kulenga mtima wa chidwi pa utumwi ndikuthandiza mamembala kumvetsetsa ntchito ya utumwi.

KUTHANDIZIRA ATUMWI

Paulo anakumbutsa mpingo ku Roma kuti ngati atumwi angakwanitse kupita kukalalikira uthenga kwa otayika, ndiye kuti wina wake awatumize (Aroma. 10:13-15). Potero, gawo lalikulu la mpingo wina uliwonse ndi kuthandiza atumwi amene ali kotumikira. Njira zitatu zimene mpingo mungachitire izi ndi kudzera mu thandizo lazachuma, thandizo la mapemphero osalekeza, komanso kupereka chisamaliro motere:

Kukhulupirika pa Kuthandiza Mchuma

Poyamba, mpingo wanu ukuyenera kumathandiza atumwi ndi chuma. Paulo amayankhula zathandizo lotero pamene anabetchera okhulupirira aku Akorinto, kuwafunsa, "Msilikali ndani achita nkhondo, nthawi ina iliyonse, nadzifunira zake yekha?" (1 Ako. 9:7). Anapitilira kuwakumbutsa, "Iwo amene alalikira Uthenga Wabwino akhale ndi moyo ndi Uthenga Wabwino" (1 Ako. 9:14).

Kuti atumwi akhalebe kumalo amene akuchita utumwi, akuyenera kumalandira thandizo la zachuma mokhulupirika ndimosadukizadukiza kuchokera kumene achokera. Thandizoli kawirikawiri limachokera kwa anthu odzipereka ndi mipingo yakumalo. Mipingo yambiri yakumalo imapereka kwa atumwi kudzera mu nthambi ya utumwi yampingo wakulikulu mdziko. Monga Mbusa, muwonetsetse kuti pali ungwiro pa zopereka zonse za utumwi ndipo kuti zikugwiritsidwa ntchito yake imene zaperekedwera.

Thandizo la Pemphero Lopitilira

Chachiwiri, mpingo upereke thandizo lapemphero losadukiza kwa atumwi awo amene ali kumalo antchito. Paulo anakumbutsa mipingo kawirikawiri kuti idzimupempherera iye. Mwachitsanzo, anawapempha Akhristu aku Tesalonika, "Chotsalira, abale, mutipempherere, kuti mau a Ambuye athamange nalemekezedwe, monganso kwanu (2 Ate. 3:1). Zitsanzo za Paulo kupempha mapemphero zikupezeka mu Aroma 15:30-32, Aefeso 6:19, Akolose 4:3-4, ndi 1 Atesalonika 5:25. Kudzera mumapemphero awo, Akhristu akhoza kuthandizira atumwi kumalo antchito kumenya nkhondo ya chikhulupiriro. Pemphero lowapemphera atumwi nthawi zina limakhudza nkhondo yolimbana ndi mizimu yoyipa (Aef. 6:11-18; Mat. 12:29).

Thandizo ndi Chisamaliro Pachikhalidwe

Pomaliza, mpingo wa Chipentekoste, ukuyenera kupereka kwa atumwi ake thandizo pachikhalidwe ndi pazokumana nazo. Atumwi nthawi zambiri amakhala kutali ndi kwawo komanso ndi amene amawathandiza. Nthawi zina amamva kuti aliwokha ndipo amafunika thandizo. Akhristu akhoza kupereka thandizoli polemba makalata ndi ma imelo olimbikitsa.

KULUNJIKA OSAFIKIRIDWA

Utumwi wa Paulo unalunjika anthu amene anali osafikiridwa. Analemba , "Ndipo kotero ndinachiyesa chinthu cha ulemu kulalikira Uthenga Wabwino, pamalopo Khristu asanatchulidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina" (Aroma. 15:20).

Mwanjira yomweyo, chikonzero chilichonse cha utumwi pampingo uliwonse wa Chipentekoste chikuyenera kuika chindunji chake pa magulu a anthu osafikiridwa. Magulu a anthu osafikiridwawa ndi mtundu kapena fuko la anthu amene alibe mayendedwe a mpingo wakumalo odzidalira. Ochita kafukufuku amati kuli mitundu ya anthu yoposa zikwi zisanu ndi ziwiri (7000) yosafikiridwa lero. Anthu osafikiridwawa akupitilira 3 biliyoni amene alibe kuthekera komva uthenga wabwino wa Yesu Khristu. Ambiri mwa anthu osafikiridwawa akupezeka ku Afirika. Mpingo wa ku Afirika ulunjike pa anthu otayikawa ndi ntchito ya utumwi.[4]

[4] Mukhoza kupeza zambiri zokhudza magulu a anthu osafikiridwawa pa webusaiti ya www.JoshuaProject.net.

~ Gawo 10 ~

MBUSA WA CHIPENTEKOSTE NDI MIYAMBO NDI MASAKARAMENTI

~ Mutu 41 ~

Kuyendetsa Mwambo wa Ukwati ndi Maliro

Atangotsiriza maphunziro ake ku sukulu ya ukachenjede, Samuel anafunsa Esther kuti amange banja ndipo iye anavomera. Pokhala anthu owopa Mulungu, anadzipereka okha kumoyo wachiyero, osagonana mpakana atalowa m'banja. Mwatsoka,asanamange ukwati wawo, kunayambika nkhondo yapachiweniweni mdziko lawo. Mabanja awo anathawira kumaiko osiyana kukabisala nkhondo. Patatha zaka ziwiri atalekana, Samuel ndi Esther anabwerera kudziko la kwawo ndipo analumikizana. Ukwati wawo sunali ofuna zinthu zambiri koma kupezeka kwa Mzimu wa Mulungu kunali pakati pawo munthawi yomanga banja lawo. Kuyambira nthawi imeneyi, Samuel ndi Esther akutumikira Ambuye mokhulupilika ndipo akuza ana oopa Mulungu.

Munkhani ina, Christopher ndi Stephen anali azichimwene ogwirizana kwambiri. Pamene Stephen anamwalira mwadzidzi, Christopher anasweka mtima. Christopher sanali m'Khristu koma m'bale wakeu. Stephen anatumikira Mulungu mokhulupirika monga dikoni mu mpingo wake. Chifukwa cha chisamaliro chimene mpingo unapereka kubanja la Stephen, ulemu munthawi ya maliro komanso abusa kuwazonda mnthawi yachisoni, Christopher ndi banja lake lonse anapereka miyoyo yawo kwa Khristu ndipo anakhala mamembala a mpingo. Lero,

Christopher ndi dikoni kumpingowo. Akutumikira pa udindo umene m'bale wake Stephen ankatumikira.

Mutu uno ufotokoza chimene Baibulo limanena zokhudza ukwati ndi maliro ndi kufunikira kwake ku banja, mpingo, ndi kudera lonse. Uperekanso nzeru kwa Mbusa wa Chipentekoste zammene angakonzekere, kuyendetsa mwambo wa maliro, ndi kutsatira omwe alowa m'banja kumene. Pamene tsatanetsatane wa mmene Mbusa angachitire miyambo imeneyi ikhoza kusiyana mmayiko osiyanasiyanso, zikhalidwe zosiyanasiyana, mutu uno upereka dongosolo la mmene mungachitire miyambo yofunikirayi posatengera kuti ndinu adziko, kapena mtundu wanji.

MWAMBO WA UKWATI

Palibe pena paliponse mu Baibulo pamene panalambedwa ndondomeko ya mmene mungachitre maukwati. Komano, limapereka zitsanzo zingapo zamaukwati ovomerezedwa ndi Mulungu. Mfundo zimene tingaziphunzire kuchokera kuzitsanzo zimenezi zikhoza kumthandizira Mbusa wa Chipentekoste kukonzekera ndi kudalitsa ukwati.

Chimodzi mwa zitsanzo zimenezi ndi nkhani ya mmene Mulungu anabweretsera limodzi Adamu ndi Hava kukhala mwamuna ndi mkazi (Genesis. 2:18-25). Atatha kuwalenga, Mulungu anawabweretsa pamodzi pachimene tikhoza kunena kuti unali "mwambo oyamba wa ukwati." Kutsatira kubwera kwao pamodzi, Baibulo limati anasandulika "thupi limodzi" (v. 24; fanizilani Mateyu 19:5-6).

Kenakano, m'buku la Genesis, Baibulo limatiuza za ukwati wa Isaki ndi Rabeka (Genesis 24:1-67). Limafotokozera momwe Mulungu anatsogolera wantchito wa Abrahamu kwa msungwana okongola wa ku Mesopotamiya otchedwa Rabeka. Atatha kumufotokozera iye chifukwa chimene anabwerera, msungwanayo anavomera kubwerera naye ku Kanani kukakhala mkazi wa Isaki. Atakumana ndi Isaki koyamba, mwaulemu anatenga chophimba chake nadziphimba kolingana ndi mwambo wanthawi imeneyo. Ndipo wantchitoyo anafotokozera Isaki mmene Mulungu anamuthandizira iye kuti apeze Rabeka. Pamenepo Isaki anatengera Rabeka ku chihema cha mayi ake Sara namkwatira kukhala mkazi wake. Anamkonda Rabeka kwathunthu natonthozedwa mwa iye. Nkhani ya Isaki ndi Rabeka imawonetsa kuti ngati wina apemphera ndi kufuna

Mulungu, adzawatsogolera kwa bwenzi lokhulupirika amena akagawana naye chimwemwe ndi chitonthozo cha banja.

Solomoni analengeza, "Wopeza mkazi apeza chinthu chabwino; Yehova amkomera mtima" (Miyambo 18:22). Kumbali inayinso, ndiyekuti ndi zoona: kuti iye amene apeza mwamuna apeza chinthu chabwino ndipo alandira kukondera kuchokera kwa Mulungu. Solomoni akutambasula choonadi ichi munyimbo, kumeneakuonetsera chithunzi chabwino cha chikondi pakati pa mwamuna ndi mkazi m'banja. Kulowa m'banja la uMulungu ndi m'dalitso.

Yesu Anadalitsa Banja

Yesu anali ndi zambiri zokamba pazakupatulika kwa banja (Mateyu 5:31-32; Marko 10:1-12). Apitilira kuonetsera mtengo umene amauyika pa banja pokakhala nawo kumwambo wa ukwati kumudzi wa Kana wa Galileya. Kumeneko, anadalitsa mwambowo pochita chozizwa chosandutsa madzi kukhala vinyo, kupulumutsa eni mwambowo kumanyazi pagulu (Yohane 2:1-11). Chifukwa chongoti ichi chinali chozizwa choyamba cha Yesu mu buku la uthenga wabwino wa Yohane zikungoonjezera kuonetsera kufunikira kumene amayika pa mwambo wa ukwati.

Kuonjezera apo, Baibulo limagwiritsa ntchito fanizo la ukwati kufotokozera ubwenzi wake wapamtima ndi anthu ake. Mwachitsanzo, m' Chipangano Chakale, Baibulo limatchula Israele monga mkwatibwi kapena mkazi wa Mulungu (Yesaya 62:5;Yeremiya 3:14). Mwa mchitidwe omwewu, mu Chipangano Chatsopano, Paulo akufotokoza mpingo ngati mkwatibwi wa Khristu (Aefeso 5:23-32). Pogwiritsa ntchito malemba owonetsera chithunzithunzi choterechi, aneneri ndi atumwi amalengeza chikondi cha Mulungu ndi kudzipereka kwake kwa anthu a Mulungu. Ndipo mwachionetsero, amalengeza mtengo umene Mulungu amayikapo pa chikhazikitso cha ukwati.

Phindu la Mwambo wa Ukwati

Ukwati wapa mpingo umapititsa patsogolo chizindikiritso chakuti ali gawo limodzi la anthu a chikhulupiriro. Amapititsanso patsogolo kudzipereka kwa awiriwa kwa wina ndi mzake. Mulungu anapanga Hava kuti athane ndi vuto la Adamu lokhala yekhayekha. Zokhudzana ndi Adamu, Mulungu adati, "sikwabwino kuti munthu akhale yekha" (Genesis. 2:18). Zomwezinso ndi zoona kwa awiri amene akwatirana kumene. Sikwabwino kuti iwo akhale okha,

kutanthauza kuti kulekanitsidwa ndi anthu okhulupirira. Monga momwe Mulungu alili Mulungu wachiyanjano cha Atate, Mwana ndi Mzimu, anamulenga munthu kuti akhale pamodzi ndi anzake.

Ku Afirika, ukwati pakati pa mwamuna ndi mkazi sichinthu chakumbali. Ndichochitika cha pagulu choti mudzi wonse usangalalire mwachimwemwe. Ukwati umaonetsera kuti awiriwo ali gawo ndi mbali ya mudzi wa okhulupirira, mpingo. Ngati mwamuna kapena mkazi ndiwakutali, chikondi ndi chisamaliro chimene banja la mpingo wawo watsopano lingawaonetsere chimawapangitsa kuti amve kulandiridwa ndi kuvomerezedwa.

Ukwati wa Chikhristu umaperekanso uthenga wa chikhalidwe ku mudzi waukulu. Banja lililonse latsopano limene lalowa m'banja mwadongosolo lake limakhala chobetchera kwa anzawo kuti atengerepo chitsanzo. Mmasiku ano m'dzikoli, ndizamanyazi kuti zakhala chikhalidwe chovomerezeka kuti mwamuna ndi mkazi akhoza kumakhala limodzi ngati okwatirana koma chonsecho sanapange mwambo wa ukwati. Iwo amene amalowa muchimangiriro cha ukwati kolingana ndi mawu a Mulungu amaonjezerapo mtengo wamakhalidwe abwino pamudzi wawo komanso amakhala chitsanzo chabwino kwa anzawo.

Kukonzekera Mwambo wa Ukwati

Kupambana kwa mwambo wa ukwati, kwambiri kumatengera kukonzekera bwino. Monga Mbusa wa Chipentekoste, muzikonzeretse nokha, komanso mkwati ndi mkwatibwi munjira zinayi:

1. Kukonzekera kwa uzimu. Choyamba, mukonze za kukonzekera kwa uzimu kwa eni ukwati. Ukwati ukuposa mgwirizano ongoti anthu azikhalira limodzi monga mmene dziko likufunira kuti ife tikhulupilire. Kuchokera mmene Mulungu amaonera zinthu, ndi pangano lopatulika pakati pa mwamuna, mkazi, ndi Mulungu. Linapangidwira mwamuna ndi mkazi amene amakhala mupangano la ubwenzi ndi Mulungu wawo. Mwambo wa ukwati uwonetsere choonadi chopatulika chimenechi.

Monga Mbusa, mupereke uphungu kwa awiriwo kuonetsetsa kuti akuzindikira kutsimikizika kwa malumbiro amene akufuna asinthane. Muonetsetse kuti mbali zonse, mkwati ndi mkwatibwi ndi obadwa mwatsopano. Ngati muzindikire kuti mmodzi mwa iwo kapena onsewo sanatembenuke mtima, mufune kuwatsogolera kwa Khristu poyambirira. Ngati ali opulumutsidwa, koma

sakukhala miyoyo yodzipereka kwathunthu, uwatsogolere kuti adziperekenso kwa Khristu

2. Kukonzekera mchikhalidwe. Chachiwiri, monga Mbusa mulingalire nkhani ya kukonzekera chikhalidwe. Mitundu yosiyanasiyana yaku Afirika ili ndi machitidwe ndi miyambo yosiyanasiyana yokhudzana ndi ukwati. Mwachitsanzo, muzikhalidwe zina, ukwati olongosoka pamayenera kuti paperekedwe kaye malowolo. Mukapezeka muzoterezi, muonetsetse kuti eniwake ukwatiwu atsatira bwino lomwe zofunikira za miyambo yotereyi tsiku la ukwati lisanafike—bola ngati zofunikirazi sizikutsutsana ndi malemba kapena malamulo a mpingo. Zikhoza kukhala zochititsa manyazi ngati sizinakonzedwe kuti zizidzafunsidwa nthawi ya mwambo waukwati mumpingo.

3. Zokonzekera za Malamulo. Chachitatu, muonetsetse kuti eniwake ukwatiwo athana nazo zonse zokhudza malamulo kolingana ndi ukwati wawo. Mwachitsanzo, muonetsetse kuti chiphaso cha ukwati chatengedwa kuchokera kwa adindo oyenelera a boma. Muonetsetsenso kuti palibe mmodzi wa iwo ali ndi mwamuna kapena mkazi wina kwina. Mmaiko ena, abusa amatha kuwayimba mlandu ngati ataphwanya malamulo a zamaukwati.

Mbusa wina analekelera udindo wake ndipo anabweretsa manyazi pa iye yekha ndi mpingo onse. Nthawi yodalitsa ukwati adanena "ngati wina angawonetse chifukwa chokwanira kuti mwamunayu asakwatire mkaziyu, ayankhule tsopano kupanda apo akhale bata kuyambira tsopano ndikale lonse." Aliyense anadabwa mzimayi wachichepere anayimika nkono. Ananena, "Sindikufuna kuyimitsa ukwatiwu, chifukwa mchemwali wanga akukwatiwa. Komabe, mwamuna amene akukwatiwa nayeyu ndi bambo wa mwana wanga. Analonjeza kuti adzandikwatira asanasinthe maganizo ake ndi kukonza zokwatira uyu." Panali chisokonezo chachikulu, pamapeto pake ukwatiwu unalephereka. Zochitika zamanyazizi zikanapewedwa abusawa akanachita kafukufuku wa mbiri ya anthuwa.

4. Kukonzekera Mwambo. Chomalizira, monga Mbusa uwonetsetse kuti mwambowo wakonzekeredwa bwino lisanafike tsiku la ukwatiwo. Ukumane ndi eniwake ukwatiwo ndikuonetsetsa kuti amvetsetsa kuti mwambo wa ukwati wa Chikhristu ndi mwambo wa kulambira ochitidwa mukupezeka kwa Mulungu.

Mavalidwe a pa ukwati a Mbusa, mkwati ndi mkwatibwi ndi onse odzakhala nawo akhale ovomerezeka mogwirizana ndimwambowo. Mkwati ndi anyamata ake ogwirizira avale molemekezeka. Mkwatibwi naye, ndi atsikana ake

othandizira ndi alendo onse achizimai avale mooneka bwino ndi moyenera. Ngati awiriwa ndi owathandizira awo asankha kuvala zovala za chikhalidwe chawo, Mbusa angafune kusinthanso zoti avale moyenera ndi mmene akwati avalira.

Mudziwiretu mtundu wa mwambo wa ukwati umene mugwiritse ntchito.[1] Muchitiretu mwambowo limodzi ndi mkwati ndi mkatibwi, kukambirana gawo lililonse la mwambowo. Potero adzazindikira kudzipereka kumene akuchita kwa wina ndi mzake. Ukwatiwu usanachitike, pabwalo komanso mkati mwa nyumba ya mpingozikonzedwe ndi kukongoletsedwa

Kumangitsa Ukwati

Mwambo wa ukwati uli mzigawo zitatu zofunikira: uthenga, kusinthana malumbiro ndi kusaina zikalata monga mwa malamulo motere:

1. Uthenga. Uthenga, kapena chilimbikitso chilunjike pakudzipereka kwa awiriwo kwa Mulungu, kukhulupilika kwawo kwa wina ndi mzake, kulera ana oopa Mulungu. Chingakhale kuti mwambowu ukulunjika awiri akulowa m'banjawo, uthenga ndi waonse amene apezeka, okwatira ndi osakwatira omwe. Uthengawo ukhale waufupi, kutenga mphindi zosaposera khumi ndi zisanu, kapena makumi awiri.

2. Mwambo. Mwambo wa ukwati weniweniwo okhudzana ndi kusinthana malumbiro ndi mphete uzindikirike ndi ulemu komanso ukhale wapaderadera. Tsiku lomanga ukwatiwu lisanafikemuyerekezere mmene zidzakhalire panthawiyo. Izi zidzathandizira kupewa kulakwitsa kochitsa manyazi patsikuli.

3. Kusainira. Monga Mbusa odzozedwa, mbali ya Mbusa wa Chipentekoste pa mwambo wa ukwati ndi ya uzimu komanso kukwaniritsa malamulo. Mukwaniritse ma udindo onse awiriwa mwa ukatswiri. Tsiku la mwambowu lisanafike, mutsimikizire kuti zikalata zonse monga mwa malamulo zilipo. Iwo amene akuyenera kusainira zikalatazi adziwitsidwiretu nthawiyi isadakwane.Uwonetsetse kuti anthu amenewa alipo ndipo akudziwa udindo wawo.

[1] Miyambo ya ukwati ikhoza kupezeka mu *Buku la Mtumiki Wotumikira,* lokonzedwa ndi Myer Pearlman. Mukhale ndi bukuli kapena lina lililonse lovomerezedwa ndi gulu la mpingo wanu.

Chomaliza, mutsogolere gawo lakusainira mu kawundula. Pamene aliyense ofunikira kusaina watero, mupereke chikalatachi pagulu kwa mkwati amene amatenga udindo waukulu pa chipambano cha ukwati. Pamene zikalata zaperekedwa, tsopano ukhoza kuwalengeza monga ngati mwamuna ndi mkazi. Muwafunse iwo awiriwa kuti agwade pamaso pa Mulungu, ngati nkotheka pamsamiro yofewa bwino. Muwasanjike manja ndikuwapempherera iwo pemphero lamdalitso. Mwambowu umatsilizika ndi mkwati kupsompsona mkwatibwi ndi mdalitso.

MWAMBO WA MALIRO

Pamene imfa ya Gertrude inalengezedwa, mzinda onse unagwedezeka. Chisoni sichinangogwira banja lake lokha koma mnzinda onse unakhuza maliro ake. Abambo, amayi, anyamata, ndi ana omwe, onse analira. Gertrude anali dikoni mumpingo wa Assemblies of God. Chifukwa cha chikhalidwe chake cha Chikhristu ndi kupereka moolowa manja kwake, anakondedwa ndi onse.

Nthawi ya maliro ake, abusa analalikira uthenga wa chitonthozo. Anagawanso uthenga wa chiyembekezo mwa Khristu. Pamapeto pa uthengawo, abusa anaitana anthu kuti alandire Khristu kukhala mpulumutsi wawo. Anthu angapo anavomera ndi kupereka miyoyo yawo kwa Khristu. Chifukwa cha moyo wa Gertrude, komanso nzeru za abusa pochititsa mwambo wa malirowo, ubwino waukulu unatuluka osangoti kuchokera kumoyo wake okha koma angakhale mu imfa yakenso.

Kufunikira kwa Mwambo wa Maliro

Anthu aku Afirika amakhala m'midzi. Makhalidwe a wina aliyense amalongosoledwa ndi kulimbikitsidwa ndi iwo amene amzungulira. Potero, wina wake akamwalira, mwambo wa maliro umabweretsa aliyense pamodzi. Anthu osiyanasiyana posatengera chipembedzo chawo amasonkhana limodzi kudzatsanzikana ndi omwalirayo. Amabweranso kudzaonetsa umodzi wawo ndi banja loferedwalo.

Mwambo wa maliro ku Afirika umakwaniritsa zinthu zingapo. Poyamba, umapereka mwai kubanja, abwenzi ndi mudzi onsepobwera pamodzi kudzalira. Pamene akuchita izi, mitima yawo imatonthozedwa ndi kulimbikitsidwa. Chotsatira, mwambo wa maliro umathandizira kupereka kwa anamalira nthawi yotseka ubale wawo ndi omwalirayo. Umawapatsa nthawi kapena malo amene

akhoza kuvomereza kuti m'bale wawo watisiya ndi kupita chitsogolo ndi miyoyo yawo mumphamvu ya Mulungu. Chomaliza, mwambo wa maliro umapereka danga labwino kwa Mbusa wa Chipentekoste kugawana uthenga wa Khristu ndi iwo amene samudziwa Iye. Ambiri amene samudziwa sangabwere kudzapemphera kumpingo patsiku lokumana koma kumaliro kokha amabwera. Mbusa wa Chipentekoste wanzeru amagwiritsa ntchito mwai oterewu mwaluso, kwinaku mokakamiza amagawana nawo anthu uthenga wachipulumutso.

Kutumikira kwa Oferedwa

Monga Mbusa wa Chipentekoste, utumiki wanu kwa anamfedwa umayamba pamene mwangomvetsedwa za imfa. Mukhale okonzeka kusokoneza mndandanda wazochita zanu ndi kuthamangira kwa okondedwa a otisiyayo. Ichi chikhala chizindikiro choyamba kubanja kuti mumawalabadira iwo. Angakhale kuti mawu achitonthozo ndi ofunikira ndi othandiza, poyambirira, osayankhula zambiri. Mungokhala ndikulira nawo limodzi banja lachisonilo. Kupezeka kwanu ndi mawu pang'ono achitonthozo, ndi pemphero ndizomwe zingafunikire panthawi imeneyi.

Kenakano, mukuyenera kukaliyenderanso banjali, nthawi iyi limodzi ndi atsogoleri ena a mpingo. Munthawi iyi, mukhoza kuyimbako nyimbo imodzi kapena ziwiri, kupereka uthenga wa chilimbikitso ndikulipemphereranso banjalo. Ukhozanso kuwerenga malemba ena oyenelera. Kupitilira apo, iwe limodzi ndi gulu la atsogoleri ako, mukhoza kupereka ndalama yachipepeso chanu m'malo mwampingo onse. Izitu zimakhala zothandiza pamene banja loferedwalo silingakwanitse kupeze chithandizo chofunikira cha malirowo.

Kukonzekera Mwambo wa Mapemphero

Inu limodzi ndi atsogoleri anu mutenge nthawi limodzi ndi banja loferedwa kukonza dongosolo la mwambo wamapemphero. Panthawi yamkumanoyi, mukhoza kugawana zochita, monga owerenga malemba ndiyemwe akalankhule za mbiri ya malemu. Mulemekeze zofuna za akubanja pa amene akufuna atachita izi. Ulaliki wa pamaliro nthawi zambiri umayenera kulalikidwa ndi Mbusa mwini nkhosa yatisiyayo. Komabe, ngati pazifukwa zina, banja loferedwa lapempha kuti mtumiki wina alalikire pa maliro mukhale ololera.

Mwambo wa Maliro

Mwambo wa maliro weniweniwo uphatikizepo zinthu zingapo zofunika. Poyamba, nyimbo zoyenerera zisankhidwe kolingana ndi mwambo wakewo. Chachiwiri, mwambowo uphatikizepo uthenga wapamaliro olalikidwa ndi Mbusa oyenerezedwa komansoolemekezeka. Ngati omwalirayo anakhala moyo wa chitsanzo uthenga ukhoza kukhala okhudzako mbiri ya moyo wake. Mosachulutsa zambiri, uthenga wachipulumutso ndi zenizeni zake za moyo ulimkudza ulalikidwe.

Mamembala ampingo ndi abwenzi aloledwe kupereka malonje awo munjira imene idzalemekeza chikumbukiro cha omwalirayo ndi kutonthoza banja loferedwa. Iwo amene akupereka malonje alimbikitsidwe kuti achite izi mwachidule kuti mwambo wa malirowu usatalike kwambiri ndi kukhalanso chipsinjo mmalo mwa mdalitso kubanja.

Mupange kuti mwambo wakumanda ukhale wachidule. Mwambo uwu nthawi zambiri umakhala ndi nyimbo, pemphero ndi mwambo oyikitsa maliro ochitidwa ndi Mbusa odzozedwa. Musunge nthawi kuonetsetsa kuti thupi la omwalirayo laikidwa mmanda bwino mdima usanagwe.

Utumiki Olondola

Udindo wanu monga Mbusa sumatha ndi kutsiriza kwa mwambo woikitsa maliro. Mukatha kuikitsa maliro, inu limodzi ndi akulu ampingo muperekeze banja loferedwa kunyumba. Kumeneko, kayankhuleni mawu omaliza achipepeso ndi kuwapempherera. Pamene masiku akupita, muzikayendera banja loferedwalo mwa apo ndi apo. Ndipo mudzisakasaka mwai ogawana nawo uthenga akubanja amene samamudziwa Ambuye.

Ukwati ndi maliro ndi nthawi zabwino kwa Mbusa wa Chipentekoste ndi mpingo kuti uwonetse chikondi ndi kukhazika kwao kwa mamembala ndi ena mmudzi. Asamalitse pokonza dongosolo ndi kuchititsa mwambo ndi chikondi mokhudzika ndi ulemu.

~ Mutu 42 ~

Kuchititsa Masakramenti, Kudalitsa Ana ndi Kukhazikitsa Atsogoleri

Mbusa wa Chipentekoste nthawi zambiri amayitanidwa kuti achititse masakramenti ampingo ndi kuchititsa miyambo ina yopatulika ndi ya chikondwerero. Zochitika izi zikuyenera kuchitidwa ndi luso komanso ulemu oyenerera. Mutu uno waperekedwa kuti uthandizire Mbusa wa Chipentekoste mudera lofunikira la utumikiwu.

UBATIZO WA M'MADZI

Ubatizo wa m'madzi ndi chimodzi mwa zoikika ziwiri zimene Yesu anazikhazikitsa. Iye mwini anabatizidwa m'madzi kukhazikitsa chitsanzo kwa amene adzamutsatire (Mateyu. 3:13-17).Analamuliranso mpingo wake kuti upite ndikupanga ophunzira mwa amitundu yonse, "ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera" (Mateyu 28:19-20; onani Marko 16:15-16).

Mpingo oyamba unatsatira malangizo a Yesu mosamalitsa pakubatiza okhulupirira oyamba m'madzi atangotembenuka mtima (Machitidwe 2:37-41; 8:12-13, 36-38; 9:17-18; 10:47-48; 16:13-15, 31-33; 18:8; 19:5). Popeza ubatizo wa mmadzi ndi lamulo la Mulungu, palibe kusankha. Potero, monga Mbusa wa

Chipentekoste, udzikonzekeretse wekha kuchititsa choikika chimenechi mokhulupirika ndi mwaukadaulo.

Tanthauzo Lake

Ubatizo wa mmadzi ndi mchitidwe omvera kumbali ya mtumiki komanso okhulupirira watsopano. Ndi chivomerezo cha pagulu cha chikhulupiriro cha ophunzira watsopano mwa Khristu ndikudzipereka kwake kukutsatira Mbuye wawo. Ubatizo mwa iwo okha supulumutsa. Komano ndi "funso lake la chikumbumtima chokoma kwa Mulungu" kuti wina wapulumutsidwa kale (1 Petro 3:21). Ubatizo wa m'madzi umaimilira imfa, kuikidwa m'manda ndi kuukanso kwa Yesu (Aroma 6:3-11). Umaimiliranso kufa kwa okhulupirira watsopanoyu kudziko ndi kuuka kwake kumoyo watsopano mwa Khristu (2 Akorinto 5:17). Kuonjezera apo, ubatizo wa m'madzi umasonyeza kudzipereka kwa okhulupirira watsopanoyu kulumikizana naye limodzi Khristu mukukwaniritsa cholinga chake (Mateyu 3:15).

Otenga Mbali

Aliyense amene wakhulupiriradi Yesu Khristu moona mtima monga Mbuye ndi Mpulumutsi wake akuyenera kubatizidwa mmadzi. Mwambowu ukuyenera kuchitika munthu atangotembenuka mtima kumene. Komabe, usanabatize wina aliyense mmadzi,umufunse kaye mafunso kuti uwonetsetse anatembenukadi mtima ndipo akumvetsetsa tanthauzo la sakramentili.

Machitidwe Ake

Njira yake ya ubatizo yam'malemba ndi kumizidwa kwathunthu m'madzi. Mau akuti "kubatiza" amatanthauza kuti kuviika kapena kumiza. Kuonjezera apo, kumizaku kukufanizira bwino mwambo ongoyerekezera imfa, kuikidwa ndi kuukanso (Aroma 6:2-4).

Ukhoza kugwiritsa ntchito ndondomeko iyi pobatiza m'Khristu watsopano. Ukhoza kumufunsa oyenera kubatizidwayu kuti anene umboni wa chipulumutso chake mwachidule. Kenakano umfunse mafunso awa:

- "Kodi uvomereza mwaufulu kuti Yesu Khristu ndi ambuye ndi Mpulumutsi wako?"
- "Kodi ukukana dziko lapansi, thupi ndi satana ndi kudzipereka kwathunthu kwa Khristu ndi chifuniro chake pa moyo wako?"

- "Kodi udzipereka wekha pamaso pa Mulungu ndi Mpingo wake kuyenda m'moyo watsopano monga kuyenera Ambuye?"
- "Kodi udzadzipereka wekha kwa Khristu ndi ntchito yake, kufunafuna kutsogolera ena kuchikhulupiriro mwa Iye?"

Ofuna kubatizidwayo ayankhe kuti "inde" kufunso lililonse

Kenakano mumize obatizidwayo mmadzi mukunena kuti, "chifukwa cha chivomerezo cha chikhulupiriro chako mwa Khristu monga Ambuye ndi Mpulumutsi wako, ndipo chifukwa chakudzipereka kwako kutaya zonse kuti umutsate Iye, ndikubatiza iwe, (tchulani dzina lake lonse), mudzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Amen."

Ndime za m'Baibulo

Mukhoza kuwerenga zina mwa ndime izi kapena zonsezi zimene zalembedwa m'baibulo panthawi ya mwambo wa ubatizo:

- Ubatizo wa Yesu (Mateyu 3:13-17; Marko 1:9-11)
- Kutuma Kwakukulu (Mateyu 28:18-20; Marko 16:14-20)
- Tsiku la Pentekoste (Machitidwe 2:36-41)
- Mdindo waku Aitiopiya (Machitidwe 8:36-39)
- Chiphunzitso cha Paulo pa ubatizo (Aroma 6:3-11; Agalatiya 3:26-29; Col. 2:11-15).

MGONERO WA AMBUYE

Mgonero wa Ambuye ndi chopatulika chachiwiri chazoikika zokhazikitsidwa ndi Ambuye Yesu (Mateyu 26:26-29; Luka 22:14-20; 1 Akorinto 11:23-26). Chimatchedwa "kunyema mkate" (Machitidwe 2:42) ndi "mgonero wa Ambuye" (1 Akorinto 11:20). Mawu akuti "chiyanjano" amachokera ku mawu a chilatini *cena,* amene amatanthauza kuti "chakudya cha madzulo." Yesu anakhazikitsa choikika ichi panthawi imene amadya chakudya chake chomaliza ndi akuphunzira ake m'chipinda cha pamwamba. Pamene ubatizo umachitika kamodzi, ndipo umayimira okhulupirira kulowa mmoyo wake watsopano mwa Khristu, mgonero umachitika kawirikawiri, ndipo umayankhula za kuyenda kopitilira kwa M'khristu ndi Ambuye.

Tanthauzo la Mgonero

Mgonero umakumbutsa okhulupirira za nsembe ya Yesu pa mtanda. Mkate onyemedwa umabweretsa chikumbukiro tha thupi lake lonyemedwa, ndi chikho, mwazi wake okhetsedwa (Luka 22:19-20). Ku 1 Akorinto 11, Paulo akuyankhula za zinthu zisanu zimene tikuyenera kumachita panthawi ya mgonero:

1. Tikuyenera kukumbukira imfa ya Khristu pa mtanda (vv. 24-25).
2. Tikuyenera kuganizira za tanthauzo la Pangano la Tsopano (v. 25; onani Mateyu. 26:28).
3. Tikuyenera kuyembekezera kudza kwake posachedwa (v. 26; onani Mateyu 26:29; Luka 22:16-18).
4. Tikuyenera kubwera pamodzi mu umodzi kukondana wina ndi mzake (vv. 18-21, 33).
5. Tikuyenera kudzipereka tokha ku cholinga cha Khristu chakuombola (v. 26).

Otenga nawo Mbali

Mipingo yambiri ya Chipentekoste imatsekula makomo kumgonero. Izi zikutanthauza kuti imalola onse amene anamulandira Khristu moonadi ngati Mpulumutsi wawo ndipo akumutumikira iye mokhulupirika kufika kugome la Ambuye. Otenga nawo mbali sakuyenera kapena kufunsidwa kukhala membala wa mpingowo kapena nthambi yake. Mipingo ina ya Chipentekoste imalola okhawo amene anabatizidwa m'madzi kudya mgonero. Inu muzindikire bwino pa malamulo amene likulu la mpingo wanu amatsatira pankhani zimenezi ndipo mutsatire machitidwe amenewo. Aliyense amene alandira mgonero alangizidwe kuti adziwunguze yekha m'mtima wake kuopa chiweruzo cha Mulungu (1 Akorinto 11:27-29).

Kuchuluka kwake

Baibulo silikupereka malangizo akuti mpingo udzikondwerera mgonero mochuluka bwanji. Komano limanena kuti mgoneroudzichitika kawirikawiri. Mipingo ina imadya mgonero lamulungu lililonse pamene ena amadya mgonero kamodzi pamwezi kapenakamodzi pa miyezi itatu. Chofunikira ndi chakuti mukhale ndi dongosolo lomadya mgonero wa Ambuye kawirikawiri.

Kachitidwe Kake

Mgonero ndi mwambo opatulika. Potero, tisachite mothamanga, tichite mwadongosolo ndi mwa ulemu wake. Mukuyenera kusankha azibambo ndi amayi a uzimu kuti akuthandizeni. Awa akhoza kukhala akulu ampingo, madikoni kapena abusa othandizira. Muwalangize otumikirawo nthawi isanakwane kuti mwambo uyenda motani.

Udzayamba mwambo ndi uthenga waufupi kapena kuwerenga malemba okhudzana ndi mgonero m'baibulo. Kenakano upemphere ndi kugawa mkate ndi makapu kwa madikoni. Madikoni agawe kwa mpingo onse. Pamene aliyense walandira mkate ndi chikho mudzawerenga ndime yoyenerera (monga 1 Akorinto. 11:23-26). Kenakano mpingo udye ndi kumwa limodzi.

Kutsatira chitsanzo cha Yesu mu Mateyu 26:26-29, mungathe kuphatikizapo zinthu zisanu pamwambowo: mayamiko, kuwerenga malemba, kugawa mgonero, kuyimba nyimbo ndi kupemphera. Mwambo wa mgonero ukhoza kuchitika panthawi ina iliyonse munthawi ya mapemphero.

Ndime za Baibulo

Mukhoza kuwerenga ndime za m'baibulo izi munthawi ya mapemphero:

- Yesu anakhazikitsa mgonero (Mateyu 26:17-29; Marko 14:12-25; Luka 22:7-20)
- Mmene mpingo oyamba umachitira (Machitidwe 2:42-46; 20:7)
- Paulo akufotokozera mgonero (1 Akorinto 10:16; 11:18-31).

MDALITSO WA ANA

Mipingo yambiri ya Chipentekoste mu Afirika imapanga mwambo odalitsa ana kwa Ambuye pagulu. Ngakhale sichoikika cha mpingo monga ngati ubatizo wam'madzi kapena mgonero, ndi m'chitidwe watanthauzo ndithu.

M'chipangano chakale, ana amaperekedwa kwa Ambuye ndikudulidwa molingana ndi chilamulo cha Mose (onani, Eksodo 13:2, 12-13, 15; 22:29; 1 Samuele 1:20, 24-28; 3:19). Hanaanampereka Samuele mwana wake wamwamuna kwa Ambuyeponena kuti "chifukwa chake inenso ndinampereka kwa Yehova; masiku onse a moyo wake aperekedwa kwa Yehova" (1 Samuele 1:28). Makolo a Yesu anatsatira mwambo wakalewu pakukamupereka Iye kwa

Ambuye (Luka 2:22-38, 40). Yesu mwini wake "anatiyangata natidalitsa, ndi kuika manja ake pa ito" (Marko 10:16).

Tanthauzo Lake

Nthawi ya mwambo, ndikofunika kutsindika kuti kupereka ana kwa Ambuye sizofanana ndi kubatiza ana. Kupereka ana sikumamupulumutsa mwanayo, kapena kumupanga kukhala m'Khristu. Ndimachitidwe ongomupatulira mwanayo kwa Ambuye basi kumbali ya makolo pamene amadzipereka okha kuti adzakuza mwanayo "m'maleredwe ndi chilangizo cha Ambuye" (Aefeso 6:4).

Kupereka mwana ndi mchitidwe owonetsera pagulu kuthokoza kwanu kwa Ambuye chifuwa cha mphatso yodabwitsa imene wapereka kwa makolo. Ndi nthawi imene msonkhano onse ukhoza kukondwera limodzi ndi makolo. Limodzi mukhoza kudziperekakumuzinga mwanayo ndi chikondi ndi kumuthandizira iye m'chikhulupiriro.

Kachitidwe Kake

Mwambo opereka mwana ukhoza kusiyana pakati pa mpingo ndi mpingo winaso komanso pakusiyana pa zikhalidwe. Nthawi zambiri zimachitika panthawi ya mapemphero a la mulungu. Ukhoza kukhala muzigawo zinayi: (1) abusa asanjike dzanja pa mwana ndikupempherera mdalitso wa Mulungu pa mwanayo; (2) abusa kupitilira kupemphera kumupempha Mulungu kuti apereke nzeru kwa makolo zokuzira mwanayo kuti atumikire Mulungu; (3) Mbusa alamule makolo, kuwalimbikitsa kuti amkuze mwanayo ndi chikondi ndi mkutumikira Ambuye ndi (4) Mbusa ayitanire pa mpingo kuti uthandize makolo kulera mwanayo munjira ya Ambuye.

Ndime za M'malemba

Ndime zotsatirazi zikhoza kuwerengedwa panthawi yopereka mwana:

- Lonjezano la Mulungu kwa Abrahamu (Genesis. 18:19)
- Phunzitsa mwana (Miyambi 22:6)
- Sindikizani malamulo a Mulungu kwa ana (Deut. 6:6-9
- Hana ampereka Samuele Kwa Ambuye (1 Samueli 1:20-2:26)
- Yesu adalitsa tiana (Mateyu 19:13-15; Marko 10:13-16; Luka 18:15-16)
- Maria ndi Yosefe apereka Yesu (Luka 2:22-38, 40)
- Kuphunzitsa ana (Aefeso 6:4).

KUKHAZIKITSA ATSOGOLERI

Chipangano Chakale komanso Chatsopano, zonse zimakambapo zokhazikitsa atsogoleri pa maudindo awo. Ambuye akulamulira Mose kuti ayeretse Aaroni ndi ana ake ku unsembe (Eksodo 29:1-27; Levitiko 8:1-36; Numeri 3:3). Kenakano anamulamulira Mose kuti achite chimodzimodzi ndi iwo Alevi amene amkatumikira ku kachisi (Numeri 8:5-22).

Mumpingo oyamba, atumwi anasanjika manja pa ma dikoni oyambirira ndikuwakhazikitsa ku ntchito yawo (Machitidwe 6:6). Chimodzimodzinso, mpingo waku Antiokeya unasanjika manja pa Barnabasi ndi Paulo kuwapereka kuntchito ya Ambuye (Machitidwe 13:2-3). Kuphatikiza apo, Paulo analamula Tito kuti ayike atsogoleri mmipingo ya mizinda yosiyanasiyana (Tito 1:5). Mneni wa Chihelene otanthauzilidwa kuti kusankha mundime imeneyi ndi *kathistēmi*, amene amatanthauza kuti "kudzoza," "kumukhazikitsa mu ofesi ya utumiki."

Mwambo okhazikitsawo udzathandiza mpingo kuti udziwe iwo amene ayikidwa m'maudindo osiyanasiya pampingopo. Udzawathandiziranso iwo kuti adziwe ntchito za mmaudindo. Udzapitirizanso kupititsa patsogolo kukhulupiriridwa kwa osankhidwawo pamaso pa mpingo. Mwambo okhazikitsawu ndi nthawinso yokumbutsa amene apatsidwa maudindo kuti ndi akapolo a Khristu, ndipo pachifukwa cha ichi, ulamuliro wake ndiongotumidwa chabe. Potero, iye si olamulira ayi, koma mtumiki wa Ambuye amene ali mwini nkhosa (1 Petro. 5:1-4).

Kachitidwe Kake

Monga Mbusa, uyambe mwambo okhazikitsawu pakuitana atsogoleri atsopano kutsogolo kwa mpingo. Kenakano uwerenge malemba ogwirizana ndi zochitikazo ndikudziwitsa adindo atsopanowo kwa mpingo onse. Mufotokoze mwachidule kumpingo ntchito za mdindo aliyense. Kenakano muwasanjike manja atsogoleriwo, kupempha Mulungu kuti awadzaze ndi Mzimu Wake ndi kuwadalitsa pamene akugwira ntchito yawo yotumikira.

Kusanjika manja nthawi iyi sikongochita chifukwa ndi mwambo wake kutero ayi. Mchipangno Chatsopano, anthu amadzazidwa ndi Mzimu Woyera pamene asanjikidwa Manja (Machitidwe 8:17; 9:17-19; 19:6). Paulo anamukumbutsa Timoteo, "ukoleze mphatso ya Mulungu ili mwa iwe mwakuyika manja." (2 Timoteo 1:6). Mtumwi amatanthauza mphatso ya Mzimu Woyera imene Timoteo analandira pa nthawi imeneyo. Mukonzekeretse atsogeleri nthawi

isanakwane powauza kuti, “Pamene ndikusanjikani manja, mutsekule mitima yanu kwa Mulungu kuti akudzazeni kapena kukudzazaninso ndi Mzimu Woyera.”

Ndime za m’Baibulo

Uwerenge ndime imodzi kapena zingapo mwa ndime izi m’Baibulo panthawi yokhazikitsa atsogoleriwa:

- Kusankha asanu ndi awiriwo (Machitidwe 6:1-7)
- Mphatso za utumiki za Khristu (1 Akorinto 12:28-31)
- Adindo amphatso za Mulungu (1 Petro 4:10-11)
- Musanyalanyaze mphatso yanu (1 Timoteo 4:9-16)
- Takasa mphatso ya Mulungu (2 Timoteo 1:1-8).

KUPEREKA ZOMANGIDWA

Kupereka Zomangidwa ndi m’chitidwe opatulika opatulira nyumba kuntchito ya Mulungu. Mchitidwe opereka nyumba kwa Ambuye umapeza tanthauzo lake m’malemba. Pa nthawi zingapo, Aisraele anapereka zomangidwa kwa Ambuye. Mchipululu, Mose ndi mpingo anapereka chihema kwa Ambuye (Eksodo 40:1-38). Anaperekanso guwa kwa Ambuye (Numeri 7:10-11, 84-88). Patapita zaka, Ezara, “Anapereka nyumba ya Mulungu mokondwera” (Ezara 6:16).

Kupereka kwa kachisi oyamba ku Yerusalemu ndi chitsanzo chabwino cha mwambo opereka m’Baibulo. Pamene Solomoni anatsiriza kumanga kachisi, anakonza mphwando la chikondwerero chachikulu (1 Mafumu 8). Nthawi yaphwando a mfumu anatsogolera mwambo opereka nyumbayi pamene anaitanira Mulungu kuti abwere ndikukhala mnyumbayo (1 Mafumu 8:13-53).

Cholinga

Lero, pamene tipereka nyumba zopemphereramo kwa Ambuye, tikuzipatulira kwa iye ndi kucholinga chake monga anachitira Mose, Ezara ndi Solomoni. Tikunena kwa Mulungu, “Tikupereka chomangidwa ichi kwa Inu, ndipo tidzachigwiritsa ntchito kubweretsa ulemerero kudzina lanu ndikupititsa patsogolo ntchito yanu padziko.”

Monga Akhristu Achipentekoste, tikuzindikira kuti Mzimu wa Ambuye amakhala mwa anthu a Mulungu (1 Akorinto 3:16), ndi kuti amawapatsa mphamvu zautumiki (Machitidwe 1:8). Komabe, tikuzindikiranso kuti kupezeka

kwa Mulungu kukhoza m'nthawi zina kubwera ndi kudzala mnyumba. Ichi ndi chimene chinachitika pa Tsiku la Pentekoste pamene, "Mwadzidzidzi anamveka mau ochokera Kumwamba ngati mkokomo wa mphepo yolimba, nadzaza nyumba yonse imene anali kukhalamo" (Machitidwe 2:2). Khristu analonjeza kuonetsera kupezeka kwake pamene awiri kapena atatu asonkhana mudzina lake (Mateyu 18:20).

Cholinga cha mwambo wa kupereka chomangidwa ndi kumuthokoza Mulungu pathandizo limene watipatsa kumpingo pakupereka kuthekera komanga ndi komalizitsa nyumba yatsopanoyo. Ndikupereka kugwiritsa ntchito nyumba yatsopano kwa iye ndi ku cholinga chake. M'mwambo wa mapempherowo, mpingo uyitane Ambuye kuti atsike ndi kudzionetsera Yekha kupezeka kwake monga anachitira m'malemba. Kuphatikiza apo, mamembala a mpingo adzipereke okha kwa Mulungu ndi ntchito yake ya chiombolo.

Mwambo Opereka Nyumba

Mwambo operekawu utsogoleredwe ndi abusa kapena muitane mtsogoleri wa mkulu wa mpingowu. Ndichabwino kuti mwambowu ukonzedwe patsiku lapaderadera limene alendo olemekezeka adzakwanitsa kudzakhala nawo. Mwambo operekawu ukhozakukhala ndi zinthu zonse izi kapena zinachabe mwa izi:

- Kudula liboni
- Pemphero lopereka nyumbayo
- Kuzindikira alendo apaderadera.
- Kuwerenga Malembo
- Maumboni
- Chikondwelero chakulambira
- Chopereka chothokoza
- Ulaliki
- Kuyendera nyumba yatsopanoyi
- Kudya limodzi kapena kumwa zoziritsa kukhosi

Ndime za M'baibulo

Ndime izi zikhoza kuwerengedwa panthawi ya mwambo opereka nyumbawu:

- Kupereka kwa Kachisi (2 Mbiri 6:1-2, 17-20, 40; 7:1-5)
- Mabwalo a Ambuye (Masalimo 84)
- Tiyeni kunyumba ya Yehova (Masalimo 122).

Kusunga masakramenti, kupereka ana, kukhazikitsa atsogoleri a mpingo, ndikupereka nyumba zopemphereramo zonse, ndi gawo limodzi lazofunikira pamoyo wa Mbusa wa Chipentekoste. Mbusa wa Chipentekoste akuyenera kuchititsa miyambo iyi mwapaderadera ndi ulemu oyenerera.

Zowonjezera

~ Zowonjezera 1 ~
Chiganizo cha Chikhulupiriro cha Chiyanjano cha Assemblies of God pa Dziko Lonse

Chiganizo cha chikhulupiriro ichi chapangidwa kuti chikhale maziko a chikhulupiriro, chiyanjano ndi mgwirizano pakati pathu. Manenedwe amene agwiritsidwe ntchito siwouziridwa koma choonadi chanenedwacho chikutengedwa kuti ndi chofunikira ku utumiki weniweni wa Chipentekoste. Palibe wanena kuti chili ndi choonadi chonse cha m'Baibulo, koma kuti chikunyamula chosowa chathu pa ziphunzitso zofunikirazi.

1. KUUZIRIDWA KWA MALEMBA

Timakhulupirira kuti malemba; Chipangano Chakale ndi Chatsopano chomwe anauziridwa ndi Mulungu ndipo ali vumbulutso la Mulungu kwa munthu, alibe cholakwika chilichonse, ndi ulamuliro odalirika pa chikhulupiriro ndi chikhalidwe. Kuuzira kwa Mulungu kukufikira mofanana komanso kwamphumphu kuzigawo zonse za zolembedwa zoyambirira, kuonetsetsa kuti ndi odalirika kwathunthu (2 Timoteo 3:15-17; 2 Petro 1:21).

2. UMULUNGU WA MUYAYA

Timakhulupirira mu umodzi wa Mulungu m'modzi oona ndi wamoyo amene ndi wamuyaya, sanalengedwe ndipo wadzizindikiritsa monga Mulungu m'modzi mwa atatu: Atate, mwana ndi Mzimu Woyera (Mateyu 3:16-17; 28:19).

a. Mulungu Atate. Timakhulupirira mwa Mulungu Atate, munthu oyamba mu utatu wa Umulungu amene akhala kwamuyaya monga Olenga kumwamba ndi dziko, opereka chilamulo, amene zinthu zonse zimumvera iye kuti akhale zonse mu zonse (Genesis 1:1; Deutoronomo. 6:4; 1 Akorinto 15:28).

b. Ambuye Yesu Khristu. Timakhulupirira mwa Ambuye Yesu Khristu, Munthu wachiwiri mu utatu wa Umulungu, amene ali mwana wa Mulungu wamuyaya amene anabadwa mthupi kudzera mwa Mzimu Woyera ndipo anabadwa mwa namwali Maria.

Timakhulupirira mu moyo wake opanda tchimo, utumiki wa zozizwa, nsembe ya imfa yake m'malo mwathu, chiukitso chake mthupi, kukwera kumwamba mwa chipambano, ndi kupembedzera kosatha (Yesaya. 7:14; Ahebri. 7:25-26; 1 Petro 2:22; Machitidwe 1:9; 2:22; 10:38; 1 Akorinto 15:4; 2 Akorinto 5:21).

c. Mzimu Woyera. Timakhulupirira mwa Mzimu Woyera, Munthu wachitatu mu utatu wa Umulungu amene achokera kwa Atate ndi Mwana, ndipo alipo nthawi zonse kuchitachita ntchito yotsutsa ndi kuperekanso moyo kwa ochimwa ndi kuyeretsa okhulupirira ku choonadi chonse (Yohane 14:26; 16:8-11; 1 Petro 1:2; Aroma 8:14-16).

3. KUGWA KWA MUNTHU

Timakhulupirira kuti munthu analengedwa wabwino ndi wangwiro. Komano, kuchimwa mwakusankha kwake kunapherezera mu kulekanitsidwa ndi Mulungu, pamene anadzitengera imfa osati yakuthupi kokha, komanso ya uzimu, imene ili kulekanitsidwa ndi Mulungu (Genesis 1:16-27; 2:17; 3:6; Aroma 5:12-19).

4. CHIPULUMUTSO CHA MUNTHU

Timakhulupirira mu chipulumutso cha kudzera mwa Khristu amena anafera machimo athu, ndipo anaikidwa m'manda, nauka kwa akufa patsiku lachitatu. Kudzera mwa mwazi wake otetezera, chipulumutso chinaperekedwa kwa anthu onse kudzera munsembe ya imfa yake pamtanda. Chochitika chimenechi chimatchedwanso kuti kubadwa kwatsopano, ndipo ndimachitachita a Mzimu Woyera nthawi yomweyo komanso okwanira pamene ochimwa amene wakhulupirira amabadwanso, kulungamitsidwa ndi kulandira umwana m'banja la Mulungu, kukhala olengedwa watsopano mwa Khristu, ndi olandira cholowa cha moyo wosatha (Yohane 3:5-6; Aroma 10:8-15; Tito 2:11, 3:4-7; 1 Yohane 5:1).

5. MACHIRITSO A UMULUNGU

Timakhulupirira kuti mamamasulidwe kumatenda anaperekedwa mu imfa ya pamtanda ndipo ndi cholowa cha okhulupirira onse (Yesaya. 53:4-5; Mateyu. 8:16-17; Yakobo 5:14-16).

6. MPINGO NDI CHOLINGA CHAKE

Timakhulupirira kuti mpingo ndi thupi la Khristu ndi pokhalapo Mulungu kudzera mwa Mzimu wake, mboni kukupezeka kwa ufumu wa Mulungu mudziko lino, ndipo umaphatikizapo onse kudziko lonse amene anabadwa kwatsopano (Aefeso 1:22-23; 2:22; Aroma 14:17-18; 1 Akorinto 4:20).

Timakhulupirira kuti cholinga cha mpingo ndi (1) kulalikira uthenga wabwino wa chipulumutso kwa anthu onse, (2)Kuumba ndikuphunzitsa okhulupirira mu utumiki. (3) kulemekeza Ambuye kudzera mukulambira ndi (4) kuonetsera chifundo cha Chikristu kwa iwo akuvutika (Mateyu 28:19-20; 10:42; Aefeso 4:11-13).

7. ZIKHAZIKITSO ZA MPINGO

Timakhulupirira kuti ubatizo wa m'madzi ndiochita kumiza munthu ndipo timayembekezera kuti onse amene analapa ndikukhulupirira akuyembekezeka kutero. Pakuchita ichi, akulengeza kudziko kuti afa ndi Khristu ndipo auka naye limodzi kuti ayende m'moyo watsopano (Mateyu 28:19; Machitidwe 10:47-48; Aroma 6:4).

Timakhulupirira kuti mgonero wa Ambuye ndi kulengezetsa masautso ndi imfa ya Ambuye wathu Yesu Khristu oti ugawidwe kwa ophunzira onse mpakana kubweranso kwa Ambuye (Luka 22:14-20; 1 Ako. 11:20-34).

8. KUYERETSEDWA

Timakhulupirira kuti kuyeretsedwa ndi mchitidwe olekanitsidwa kuchimene chili choipa, ndi kudzipereka kwa Mulungu. Pa zimene zimatichitikira, ndizoti zimachitika nthawi yomweyo komanso zimachitika mopitilira nthawi ndi nthawi. Kumachitika m'moyo wa okhulupirira pamene akugwiritsa ntchito mphamvu ya Mwazi wa Khristu ndi moyo wakuuka kwake kudzera mu umunthu wa Mzimu Woyera. Amakopa chidwi cha okhulupirira, kumphunzitsa kudzera m'mau ndi kuumba chikhalidwe cha Khristu mkati mwake (Aroma. 6:1-11; 8:1-2, 13; 12:1-2; Agalatiya. 2:20; Ahebri. 10:10, 14).

9. UBATIZO WA MZIMU WOYERA

Timakhulupirira kuti ubatizo wa Mzimu Woyera ndiko kukhazikitsa mphamvu pa okhulupirira kuti akhale moyo ndi kutumikira Khristu. Chochitika ichi ndi chosiyana ndipo chimatsatira kubadwa kwatsopano, kumalandiridwa mwa chikhulupiriro, ndipo kumatsatidwa ndi chionetsero choyankhula malilime monga Mzimu awayankhulitsa ngati chizindikiro choyambayamba (Luka 24:49; Machitidwe 1:8; 2:1-4; 8:15-19; 11:14-17; 19:1-7).

10. MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Timakhulupirira kuti mphatso za Mzimu Woyera zisanu ndi zinai zidakagwirabe ntchito masiku ano (1 Akorinto 12) ndi mphatso za utumiki za Khristu (Aefeso 4:11-13) kukumangilira ndi kukula kwa mpingo.

11. CHIMALIZIRO CHA NTHAWI

Timakhulupirira mukubweranso kwake kwa Yesu mwansanga mthupi kudzasonkhanitsa anthu ake kwa iye yekha isanafike nthawi ya ulamuliro wake wa zaka chikwi. Pokhala nacho chiyembekezo ichi ndi kudikilira kotere, tidziyeretsa tokha, angakhale monga iye ali oyera, kuti tikhale okonzeka kukumana naye pamene adza (Yohane 14:1-3; Tito 2:13; 1 Atesalonika 4:15-17; 1 Yohane 3:2-3; Chivumbulutso 20:1-6).

Timakhulupilra kuuka mthupi kwa anthu onse, ozindikira mchikondwelero chosatha kwa onse amene akhulupiriradi mwaAmbuye wathu Yesu Khristu ndi mozindikira mchilango chosatha kwa kukhala gawo la onse amene maina awo sanalembedwe m'buku la amoyo (Yohane 5:28-29; 1 Akorinto 15:22-24; Chivumbulutso 20:10-15).

~ Zowonjezera 2 ~
Mphatso Zowonekera za pa 1 Akorinto 12:8-10

Mphatso Za Mavumbulutso (Zoperekedwa kuti tidziwe malingaliro a Mulungu)

- *Mau (Uthenga) a chidziwitso:* Vumbulutso loperekedwa ndi Mzimu la gawo la chidziwitso cha Mulungu
- *Mau (uthenga) a nzeru:* Vumbulutso la nusu ya nzeru ya Mulungu yoperekedwa ndi Mzimu
- *Kusiyanitsa Mizimu:* Vumbulutso lozindikira kuti ndi mzimu wanji umene ukuonetsedwa kapena kumutakasa wina kuchita zinthu

Mphatso za Uneneri (zoperekedwa kuti tidziwe mau a Mulungu)

- *Mphatso ya uneneri:* Kuyankhula kotakasidwa ndi Mzimu kupereka uthenga ochokera kwa Mulungu
- *Malilime a mitundu mitundu:* Kuyankhula kotakasidwa ndi Mzimu kwa uthenga kuchokera kwa Mulungu kapena pemphero kwa Mulungu muchiyankhulo chosadziwika ndi oyankhulayo
- *Kutanthauzira malilime:* Kuyankhula kotakasidwa ndi Mzimu kupereka tanthauzo ku uthenga kapena pemphero lonenedwa m'malilime.

Mphatso za Mphamvu (Zoperekedwa kuti tikachite ntchito ya Mulungu)

- *Mphatso ya Chikhulupiriro:* Chikhulupiriro chopatsidwa mphamvu/kutakasidwa ndi Mzimu Woyera kuti ukwaniritse ntchito yoyikidwa ndi Mulungu.
- *Mphatso za Machiritso:* Kuchiritsidwa kwa matenda ndi zifooko kopatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera
- *Mphamvu ya Zozizwa:* Kuthekera komasula mphamvu ya Mulungu koperekedwa ndi Mzimu Woyera kuti ikwaniritse ntchito yapaderadera ya Mulungu. (Dziwani: Mphatso iyi ikhozanso kutchulidwa kuti "Machitidwe Mwa mphamvu") kapena monga momwe zinalembedwera mchihelene(*energemata dunameon*) "Machitachita antchito zamphamvu."

~ Zowonjezera 3 ~
Chidule cha Mabuku a M'baibulo

Chipangano Chakale

Genesis	Gen.
Eksodo	Eks.
Levitiko	Lev.
Numeri	Num.
Deuteronomo	Deut.
Yoswa	Yos.
Oweruza	Ower.
Ruth	Rut.
1 Samuele	1 Sam.
2 Samuele	2 Sam.
1 Mafumu	1 Maf.
2 Mafumu	2 Maf.
1 Mbiri	1 Mbi.
2 Mbiri	2 Mbi.
Ezara	Ezr.
Nehemiya	Neh.
Estere	Est.
Yobu	Yob.
Masalimo	Mas.
Miyambo	Miy.
Mlaliki	Mlal.
Nyimbo ya Solomoni	Nyi.
Yesaya	Yes.
Yeremiya	Yer.
Maliro	Mali.
Ezekiele	Eze.
Daniele	Dan.
Hoseya	Hos.
Yowele	Yow.
Amosi	Amo.
Obadiya	Oba.
Yona	Yon.
Mika	Mik.
Nahumu	Nah.
Habakuku	Hab.
Zefaniya	Zef.
Hagai	Hag.
Zekariya	Zek.
Malaki	Mal.

Chipangano Chatsopano

Mateyu	Mat.
Marko	Mrk.
Luka	Luk.
Yohane	Yoh.
Machitidwe A Atumwi `	Mach
Aroma	Aro.
1 Akorinto	1 Ako.
2 Akorinto	2 Ako.
Agalatiya	Agal.
Aefeso	Aef.
Afilipi	Afi.
Akolose	Ako.
1 Atesalonika	1 Ate.
2 Atesalonika	2 Ate.
1 Timoteo	1 Tim.
2 Timoteo	2 Tim.
Tito	Tit.
Filemoni	File.
Ahebri	Aheb.
Yakobo	Yak.
1 Petro	1 Pet.
2 Petro	2 Pet.

1 Yohane	1 Yoh.	Yuda	Yud.
2 yohane	2 Yoh.	Chivumbulutso	Chiv.
3 Yohane	3 yoh.		

AFRICA'S
HOPE